# Buku Loyera La Korani

CHICHEWA

# Buku Loyera La
# Korani

Lomasuliridwa M'Chichewa

Lomasuliridwa ndi
Mufti Al Haji Yusuf Muhammad Kanyamula

GOODWORD

First Published 2018
This book is Copyright free

Goodword Books
A-21, Sector 4, Noida-201301, India
Tel. +9111-46010170, +9111-49534795
Mob. +91-8588822672
email: info@goodwordbooks.com
www.goodwordbooks.com
www.cpsglobal.org

Chennai
Mob. +91-9790853944, 9600105558

Printed in India

# Contents

| | |
|---|---|
| Sura 1 • Al-Fâtiha (Al-Fatiha) | 7 |
| Sura 2 • Al-Ba'karah (Al-Baqara) | 7 |
| Sura 3 • Al 'Imrân (Al Imran) | 54 |
| Sura 4 • An-Nisâ (Al Nisa) | 82 |
| Sura 5 • Al-Mâ-idah (Al Maidah) | 110 |
| Sura 6 • Al-An'âm (Al-Anam) | 132 |
| Sura 7 • Al-A'râf (Al A'raf) | 156 |
| Sura 8 • Al-Anfâl (Anfal) | 182 |
| Sura 9 • At-Tawbah (At-Tauba) | 192 |
| Sura 10 • Yûnus (Yunus) | 212 |
| Sura 11 • Hûd (Hud) | 226 |
| Sura 12 • Yûsuf (Yusuf) | 242 |
| Sura 13 • Ar-Ra'd (Al-Ra'd) | 256 |
| Sura 14 • Ibrâhîm (Ibrahim) | 263 |
| Sura 15 • Al-Hijr (Al-Hijr) | 270 |
| Sura 16 • An-Nahl (Al-Nahl) | 276 |
| Sura 17 • Al-Isrâ' (Bani Israel) | 292 |
| Sura 18 • Al-Kahf (Al-Kahf) | 305 |
| Sura 19 • Maryam (Marium) | 318 |
| Sura 20 • Tâ-Hâ (Ta Ha) | 326 |
| Sura 21 • Al-Anbiyâ' (Al-Anbiya) | 338 |
| Sura 22 • Al-Hajj (Al-Haj) | 348 |
| Sura 23 • Al-Mu'minûn (Al-mu-minun) | 359 |
| Sura 24 • An-Nûr (Al Nur) | 368 |
| Sura 25 • Al-Fur'kân (Al Furqan) | 378 |
| Sura 26 • Ash-Shu'arâ (Al Shuara) | 386 |
| Sura 27 • An-Naml (Al Naml) | 397 |

Sura 28 • Al-‘Kasas (Al Qasas) 407
Sura 29 • Al- Ankabût (Ankabut) 418
Surah 30 • Ar-Rûm (Al Rum) 427
Sura 31 • Lu‘kmân (Luqman) 434
Sura 32 • Sajdah (Sajda) 438
Sira 33 • Al-Ahzâb (Al Ahzab) 441
Sura 34 • Saba (Al Saba) 452
Sura 35 • Al-Fâtir (Al Fatir) 459
Sura 36 • Yâsîn (Ya Seen) 466
Sura 37 • As-Sâffât (Al Saffat) 472
Sura 38 • Sâd (Al Suad) 480
Sura 39 • Az-Zumar (Al Zumar) 487
Sura 40 • Al-Mu’min (Mu-Min) 497
Sura 41 • Fussilat (Fussilat) 506
Sura 42 • Ash-Shûra (Ash-Shura) 513
Sura 43 • Az-Zurhruf (Zukhruf) 521
Sura 44 • Ad-Durhân (Ad-Dukhan) 528
Sura 45 • Al-Jâthiyah (Al Jasiyah) 532
Sura 46 • Al-Ah’kâf (Al Ahqaf) 536
Sura 47 • Muhammad (Muhammad) 541
Sura 48 • Al-Fath (Al Fateh) 547
Sura 49 • Al-Hujurât (Al Hujurat) 552
Sura 50 • ‘Kâf (Qaf) 555
Sura 51 • Ad-Dhâriyât (Zariat) 558
Sura 52 • At-Tûr (Al Tur) 561
Sura 53 • An-Najm (Al Najm) 565
Sura 54 • Al-’Kamar (Qamar) 568
Sura 55 • Ar-Rahmân (Rahman) 572
Sura 56 • Al-Wâ’ki’a (Al Waqia) 575

Sura 57 • Al-Hadîd (Al Hadid) 579
Sura 58 • Al-Mujâdilah (Al Mujadilah) 584
Sura 59 • Al-Hashr (Al Hashr) 588
Sura 60 • Al Mumtahanah (Al Mumtahana) 592
Sura 61 • As-Saff (As-Saff) 596
Sura 62 • Al-Jumu'ah (Al Jumua) 598
Sura 63 • Al-Munâfi'kûn (Al Munafiqun) 600
Sura 64 • At-Tagrhâbun (Al Taghabun) 602
Sura 65 • At-Talâ'k (Al Talaq) 604
Sura 66 • At-Tahrîm (Al Tahrim) 607
Sura 67 • Al-Mulk (Al Mulk) 609
Sura 68 • Al-'Kalam (Al Qalam) 612
Sura 69 • Al-Ha'k'kah (Al Haqqa) 615
Sura 70 • Al-Ma'ârij (Al Ma'arij) 618
Sura 71 • Nûh (Nuh) 620
Sura 72 • Al-Jînn (Al Jinn) 622
Sura 73 • Al-Muzzammil (Al Muzzammil) 625
Sura 74 • Al-Muddath-thir (Al Muddaththir) 627
Sura 75 • Al-'Kiyâmah (Qiyamah) 629
Sura 76 • Al-Insân (Al Insan) 631
Sura 77 • Al-Mursalât (Al Mursalat) 634
Sura 78 • An-Nabâ (Al-Naba) 636
Sura 79 • An-Nâzi`ât (Al-Naziat) 638
Sura 80 • 'Abasa (Abasa) 640
Sura 81 • At-Takwir (Al-Takwir) 641
Sura 82 • Al-Infitâr (Infitar) 643
Sura 83 • Al-Mutaffifîn (Al Mutaffifin) 644
Sura 84 • Al-Inshi'kâ'k (Al-Insiqaq) 646
Sura 85 • Al-Burûj (Al-Buruj) 647

Sura 86 • At-Târi`k (Tariq) 648
Sura 87 • Al-A`laa (Al-A'la) 649
Sura 88 • Al-Grhâshiyah (Al-Ghashiya) 650
Sura 89 • Al-Fajr (Al Fajr) 651
Sura 90 • Al-Balad (Al Balad) 652
Sura 91 • A-sh-Shams (Al-Shams) 653
Sura 92 • Al-Layl (Al-Layl) 654
Sura 93 • Ad-Dhuha (Al-Dhuha) 655
Sura 94 • Ash-Sharh (Al-Inshirah) 656
Sura 95 • At-Tin (Al-Tin) 656
Sura 96 • Al-'Ala`k (Al-Alaq) 657
Sura 97 • Al-'Kadr (Al-Qadri) 658
Sura 98 • Al-Bayyina (Al-Bayyina) 658
Sura 99 • Az-Zilzâl (Al-Zalzala) 659
Sura 100 • Al-'Adiyât (Al-Adiyat) 660
Sura 101 • Al-'Kâriyah (Al-Qaria) 661
Sura 102 • At-Takâthur (Al-Takthur) 661
Sura 103 • Al-'Asr (Al-Asr) 662
Sura 104 • Al-Humâzah (Al-Humaza) 662
Sura 105 • Al-Fîl (Al Fil) 663
Sura 106 • Al-'Kuraysh (Al-Qurysh) 663
Sura 107 • Al-Ma`ûn (Al-Maun) 664
Sura 108 • Al-Kawthar (Al-Kawthar) 664
Surah 109 • Al-Kâfirûn (Al-Kafiruni) 665
Sura 110 • An-Nasr (Al-Nasr) 665
Sura 111 • Lahab (Al-Lahab) 666
Sura 112 • Al-Ikhlâs (Al-Ikhlas) 666
Sura 113 • Al-Fala`k (Al-Falaq) 667
Sura 114 • An-Nâs (Al Anas) 667

Sura 1 • Al-Fâtiha

# Al-Fatiha

1. M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

2. Kuyamikidwa ndi kwa Mulungu, Ambuye wa chilengedwe.
3. Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha. 4. Mfumu
ya tsiku la Chiweruzo. 5. Inu nokha tikulambirani ndipo
ndi kwa Inu nokha kumene timapempha chithandizo.
6. Tilangizeni njira yanu yoyenera. 7. Njira ya iwo amene
mwawakonda osati ya iwo amene adalandira mkwiyo wanu
kapena anasokera.

Sura 2 • Al-Ba'karah

# Al-Baqara

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha.

1. *Alif Lam Mim*

2. Ili ndi Buku limene mulibe chokaikitsa, ulangizi kwa
anthu oopa Mulungu. 3. Amene amakhulupirira mu
chinthu chosaoneka ndipo amapemphera pa nthawi
yake ndipo amapereka kwa anthu osowa zina mwa
zinthu zimene tawapatsa. 4. Ndi amene amakhulupirira
mu zimene zavumbulutsidwa kwa iwe ndiponso
zimene zinavumbulutsidwa kale iwe usanadze ndipo
amakhulupirira kwathunthu m'moyo umene uli nkudza.

5. Amenewa ndiwo amene ali pa njira yoyenera ya Ambuye
wawo ndipo ndiwo opambana.
6. Ndithudi iwo amene sakhulupilira ndi chimodzimodzi
kwa iwo kaya iwe uwachenjeza kapena osawachenjeza,
ndipo iwo sadzakhulupilira. 7. Mulungu waika chophimba
m'mitima mwawo ndi m'makutu mwawo, ndi m'maso
mwawo muli chovindikira. Ndipo chawo chidzakhala
chilango chachikulu.
8. Pakati pa anthu alipo amene amanena kuti: "Ife
tikhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku la chiweruzo"
pamene iwo sali anthu okhulupirira ngakhale pang'ono.
9. Iwo amangofuna kunamiza Mulungu ndi iwo amene
amakhulupirira mwa Iye. Koma iwo sanamiza wina
aliyense kupatula kudzinamiza okha ngakhale kuti iwo
sazindikira. 10. M'mitima mwawo muli matenda ndipo
Mulungu wawonjezera. Iwo adzalangidwa kwambiri
chifukwa cha chinyengo chawo. 11. Ndipo zikanenedwa
kwa iwo kuti: "Musachite zoipa m'dziko," iwo amayankha
kuti: "Ndithudi ife ndi ochita zabwino." 12. Ndithudi! Iwo
ndiwo amene amachita zoipa koma kuti iwo sazindikira.
13. Ndipo zikanenedwa kwa iwo kuti: "Khulupiriranі monga
momwe anthu akhulupirira." Iwo amayankha kuti: "Kodi
ife tikhulupirire monga momwe zitsiru zikhulupirira?"
Ndithudi iwo ndiwo zitsiru koma iwo sazindikira.
14. Ndipo iwo akakumana ndi anthu okhulupirira, amanena
kuti: "Ife timakhulupilira!" Koma akakhala okha pakati pa
a Satana awo amati: "Ndithudi ife tili ndi inu. Ndithudi ife
timangowasyasyalika chabe." 15. Mulungu amawasyasyalika
iwo ndipo amawasiya nthawi yaitali mu uchimo ndi
kumapitiririrabe kuchimwa mwaumbuli. 16. Amenewa

ndiwo amene agula chisokonekero m'malo mwa njira
yoyenera. Iwo sanapindule pa malonda awo. Ndipo sanali
wotsogozedwa.
17. Iwo ali ngati munthu amene adasonkha moto ndipo
pamene moto unali nkuyaka, kuunika zimene zili m'mbali
mwake, Mulungu anachotsa kuwala kwawo ndipo
adawasiya ali mu mdima waukulu wosathanso kuona. 18. Iwo
ndi osamva, osalankhula ndi osaona ndipo sadzabwerera
ku njira yoyenera. 19. Kapena ali ngati mvula ya mkuntho
imene mkati mwake muli mdima, kugunda ndi ziphaliwali.
Ndipo amatseka zala m'makutu mwawo akamva kugunda
chifukwa choopa imfa. Koma Mulungu amawadziwa
bwino anthu onse osakhulupirira. 20. Mphenzi, pafupifupi,
imawalanda kuona. Nthawi iliyonse imene iyo ing'anipa
iwo amayenda ndipo kukakhala mdima iwo amaima. Ndipo
ngati Mulungu akadafuna akadawalanda kumva ndi kuona
kwawo. Ndithu Mulungu ali ndi mphamvu pa zinthu zonse.
21. Oh inu anthu! Pembedzani Ambuye wanu, amene
adakulengani inu ndi iwo amene adalipo kale kuti mukhale
angwiro. 22. Iye adapanga dziko lapansi kukhala malo anu
a mpumulo ndi mtambo ngati chokuta. Ndipo anatumiza
mvula kuchokera kumwamba ndi kubweretsa kwa inu
zipatso ngati zakudya zanu. Motero musakhale ndi milungu
ina mowonjezera pa Mulungu m'modzi yekha pamene
muli kudziwa. 23. Ngati inu muli ndi chikayiko pa zimene
tavumbulutsa kwa kapolo wathu, bweretsani mutu umodzi
wolingana ndi imene ili m'buku ili ndipo itanani mboni zanu
kupatula Mulungu ngati muli kunena zoona. 24. Koma ngati
inu simubweretsa ndipo simudzabweretsa (mboni) motero
opani moto umene nkhuni zake ndi anthu ndi miyala,

umene wasonkhedwera anthu osakhulupirira. 25. Ndipo
auze nkhani yabwino iwo amene ali ndi chikhulupiriro
ndipo amachita ntchito zabwino kuti iwo adzakhala
m'minda yothiriridwa ndi madzi a m'mitsinje yoyenda.
Nthawi zonse akapatsidwa zipatso zochokera m'mindayo,
iwo adzati: "Izi ndi zimene tinapatsidwa kale." Chifukwa
iwo adzapatsidwa zofanana nazo ndipo iwo adzakhala ndi
akazi osakhuzidwa ndipo adzakhala kumeneko mpaka
kalekale.
26. Ndithudi Mulungu sachita manyazi kupereka fanizo
la kanthu kakang'ono ngati udzudzu kapena chinthu
chachikulu. Koma anthu okhulupirira amadziwa kuti ndi
choonadi chochokera kwa Ambuye wawo pamene anthu
osakhulupirira amati: "Kodi Mulungu akufuna kutanthauza
chiyani mufanizo ili?" Kudzera m'mafanizo otere Mulungu
amasocheza anthu ambiri ndiponso amatsogolera anthu
ambiri. Ndipo Iye sasokeza wina aliyense kupatula
okhawo ochita zoipa. 27. Amene amaswa lonjezo la
Mulungu pambuyo pomanga ndipo amatayanitsa zinthu
zimene Mulungu walamulira kuti zilumikizidwe ndiponso
amachita zoipa m'dziko. Iwowo ndi anthu olephera.
28. Kodi inu simungamukhulupilire Mulungu bwanji? Poona
kuti inu munali akufa, Iye adakupatsani moyo ndipo Iye
adzakuphani ndipo adzakupatsaninso moyo ndipo kwa
Iye mudzabwerera. 29. Iye ndiye amene adakulengerani inu
zinthu zonse zimene zili padziko lapansi. Ndipo atatero
analenga kumwamba ndipo adalenga miyamba isanu ndi
iwiri ndipo Iye ndi wodziwa chinthu china chilichonse.
30. Ndipo pamene Ambuye wako adati kwa angelo: "Ine
ndiika olamula padziko lapansi." Iwo adati: "Kodi inu

mudzaika padziko amene adzakhala ali kuchita zoipa ndi
kukhetsa mwazi pamene ife tili kuyamika ndi kutamanda
ulemerero wanu?" Iye adati: "Ine ndimadziwa zimene inu
simudziwa."

31. Ndipo Iye adamuphunzitsa Adamu mayina a zinthu
zonse ndipo adazisonkhanitsa pamaso pa angelo nati:
"Ndiuzeni mayina a zinthu izi ngati ndinu achilungamo."
32. Iwo adati: "Ulemerero ukhale kwa Inu. Ife tilibe nzeru
kupatula zokhazo zimene mutiphunzitsa. Ndithudi Inu
nokha ndinu amene muli Wodziwa ndi Wanzeru." 33. Ndipo
Mulungu adati: "Iwe Adamu! Auze mayina ake." Ndipo
pamene iye adatchula mayina a zinthuzo, Mulungu adati:
"Kodi Ine sindidakuuzeni inu kuti Ine ndimadziwa zobisika
za kumwamba ndi za dziko lapansi ndipo ndimadziwanso
zonse zimene inu mumaulula ndi zimene mumabisa?"

34. Ndipo pamene Ife tidati kwa angelo: "Mugwadireni
Adamu." Ndipo onse adamugwadira kupatula Satana
amene adakana ndi kudzikweza ndipo adakala m'modzi
wa osakhulupilira. 35. Ndipo Ife tidati: "Oh Adamu! Khala
iwe pamodzi ndi mkazi wako m'mundamo ndipo muzidya
mmene mungafunire koma musadzayandikire mtengo
uwu chifukwa mudzakhala anthu ochimwa." 36. Koma
Satana adawanyenga ndipo adawachotsetsa m'munda
m'mene iwo adali. Ife tidati: "Tsikani pansi nonse ndipo
inu mudzakhala mdani wa wina ndi mnzake. Ndipo dziko
lapansi ndi kumene inu mudzakhala ndi chisangalalo cha
kanthawi kochepa." 37. Ndipo Adamu adalandira mawu
kuchokera kwa Ambuye wake. Ndipo Ambuye wake
adamukhululukira iye. Ndithudi Iye ndi wokhululukira
ndi Mwini chisoni chosatha. 38. Ife tidati: "Tsikani pansi

nonsenu ndipo pamene Ulangizi wanga udzakufikani, yense
amene adzatsatira Ulangiziwu, iye sadzakhala ndi mantha
ndipo sadzadandaula." 39. Koma iwo amene sakhulupilira
ndipo amatsutsa zizindikiro zathu, iwo adzakhala eni ake a
ku Gahena ndipo adzakhalako mpaka kalekale.

40. Oh Inu ana a Israeli! Kumbukirani madalitso anga
amene ndidakupatsani inu ndipo kwaniritsani lonjezo langa
ndipo Ine ndikwaniritsa lonjezo lanu. Ndipo ndiopeni Ine
ndekha. 41. Ndipo khulupirirani mu zimene ndatumiza
zimene zichitira umboni chivumbulutso chimene muli
nacho, kotero inu musakhale anthu oyamba kuzikana,
ndipo musagule ndi mau anga kanthu kakang'ono. Ndipo
ndiopeni Ine ndekha. 42. Ndipo musasakanize choonadi
ndi bodza, ndi kubisa choonadi pamene muli kudziwa.
43. Ndipo pempherani pa nthawi yake, perekani chopereka
ndipo weramani pamodzi ndi iwo amene ali kuwerama.
44. Kodi inu mumauza anthu kuchita zabwino pamene
inu simulabadira kutero ngakhale mumawerenga Mau
a Mulungu? Kodi mulibe nzeru? 45. Funani chithandizo
popirira ndi popemphera. Ndithudi izi ndi zovuta kupatula
kwa anthu okhulupilira. 46. Iwo amene amadziwa kuti
adzakumana ndi Ambuye wawo ndipo kuti ndi kwa Iye
kumene adzabwerera.

47. Oh inu ana a Israeli! Kumbukirani madalitso anga
amene ndidakupatsani inu ndipo kuti ndidakukondani inu
kuposa mitundu ina yonse. 48. Ndipo opani tsiku limene
munthu sadzatha kuthandiza mnzake kapena kupepesa
ndipo dipo silidzalandiridwa ndiponso sadzathandizidwa.
49. Ndi mmene tidakupulumutsirani kwa anthu a Farawo,
amene anali kukuzunzani kwambiri popha ana anu a

amuna ndi kusiya ana anu a akazi. Ndithudi amenewa
adali mayeso ochokera kwa Ambuye wanu. 50. Ndi pamene
Ife tidagawanitsa nyanja ndi kukupulumutsani inu ndipo
tidamiza anthu a Farawo inu muli kuona. 51. Ndi pamene
tidamusankhira Mose masiku makumi anayi ndipo inu
mudakonza fanizo la ng'ombe kotero inu mudachimwa.
52. Zitatero, Ife tidakukhululukirani ndi cholinga chakuti
mwina mukhoza kuthokoza. 53. Ndi pamene Ife tidamupatsa
Mose Buku ndi nzeru kuti mutsogozedwe. 54. Ndi pamene
Mose adati kwa anthu ake: "Oh inu anthu anga! Ndithudi
inu mwadzilakwitsa nokha popembedza fano la mwana
wa ng'ombe. Lapani kwa Ambuye wanu ndipo mudziphe
nokha. Zimenezo zidzakhala zabwino kwa inu pamaso pa
Ambuye wanu." Ndipo Iye adzakukhululukirani inu. Iye
ndi Mwini chikhululukiro ndi Mwini chisoni chosatha. 55.
Ndi pamene inu munati: "Oh Mose! Ife sitidzakukhulupilira
iwe pokhapokha titamuona Mulungu ndi maso athu."
Nthawi yomweyo chilango chidakufikirani inu muli kuona.
56. Kenaka Ife tidakuukitsani kwa akufa kuti mwina
mukhale othokoza. 57. Ndipo tidalamula mtambo kuti
ukukuteni ndipo tidakutumizirani Manna ndi Mbalame,
ndipo tidati: "Idyani zinthu zabwino zimene takupatsani."
Ndipo iwo sadatilakwire Ife ayi koma adadzilakwira okha.

58. Ndi pamene tidawauza kuti: Lowani mu Mzinda
uwu ndipo mudye mmenemo mosangalala ndi momwe
mungafunire. Lowani modzichepetsa pachipata
ndipo munene kuti: "Tikhululukireni" ndipo Ife
tidzakukhululukirani machimo anu ndipo tidzawaonjezera
zabwino anthu onse ochita zabwino. 59. Koma anthu ochita
zoipa adasintha mawu amene adanenedwa kwa iwo ndipo

tidawaponyera, ngati chilango, mlili ochokera kumwamba
chifukwa cha zolakwa zawo. 60. Ndi pamene Mose adafunsa
madzi oti apatse anthu ake, Ife tidamuuza kuti: “Menya
mwala ndi ndodo yako!” Ndipo nthawi yomweyo a kasupe
khumi ndi awiri adatumphuka. Ndipo pfuko lililonse
lidadziwa malo ake omwera. Ife tidati: “Idyani ndipo imwani
koma musayambitse chisokonezo m'dziko pochita zoipa.”
61. Ndi pamene mudati: “Oh Mose! Ife sitingapirire kudya
chakudya chamtundu umodzi. Motero tipemphere kwa
Ambuye wako kuti atitulutsire zina mwa zomera m'nthaka
monga masamba, minkhaka, tirigu, nyemba ndi anyezi.”
Iye adati: “Kodi inu mufuna kusinthitsa chinthu chabwino
ndi choipa? Pitani ku mzinda uliwonse ndipo kumeneko
mudzapeza zonse zimene mufuna.” Ndipo manyazi ndi
umphawi udadza pa iwo ndipo iwo adapalamula mkwiyo
wa Mulungu chifukwa iwo adali kukana mau a Mulungu
ndipo anali kupha Atumwi popanda chifukwa popeza iwo
adali anthu aupandu ndi anthu osamvera.

62. Ndithudi iwo amene amakhulupirira ndi iwo amene
ali Ayuda, Akhiristu ndi Asabiyani, aliyense amene
amakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza ndipo
amachita ntchito zabwino, adzalandira malipiro ake
kuchokera kwa Ambuye wawo. Iwo alibe china chili chonse
choti aope kapena kudandaula.

63. Ndi pamene Ife tidachita pangano ndi inu ndipo
tidakweza phiri kuti likhale pa inu. Ndipo tidati: “Landirani
lamulo limene takupatsani inu ndipo kumbukirani
zonse zili mmenemo kuti mukhale olungama.” 64. Ndipo
zitatero inu mudabwerera m'mbuyo. Koma pakadapanda
chisomo ndi chisoni cha Mulungu pa inu, ndithudi inu

mukadakhala mgulu la anthu osochera. 65. Ndipo, ndithudi,
inu mudadziwa za anthu amene adaswa malamulo a tsiku
la Sabata. Ife tidawauza kuti: “Khalani anyani, onyozedwa
ndi okanidwa.” 66. Motero tidapereka chilango ichi ngati
chitsanzo kwa anthu a mtundu wawo ndi onse amene adali
kuwatsatira ndi phunziro kwa anthu angwiro.
67. Ndi pamene Mose adati kwa anthu ake: “Mulungu
wakulamulani kuti muphe ng’ombe.” Iwo adati: “Kodi
iwe ufuna kutichita chipongwe?” Mose adati: “ Ndithudi
Mulungu anditeteze kuti ndisakhale mbuli.” 68. Iwo adati:
“Pempha kwa Ambuye wako kuti atiuze ife za mtundu
wa ng’ombe”. Mose adati: “Ndithudi Ambuye wanu akuti
ng’ombeyi isakhale yokalamba kapena yaing’ono koma
kuti ikhale pakati ndi pakati ndipo chitani chimene
mwalamulidwa.” 69. Iwo adati: “Pempha kwa Ambuye wako
kuti atiuze ife maonekedwe a ng’ombeyo”. Mose adati:
“Ambuye wanu akuti ng’ombeyo ndi yachikasu yowala
ndi yokondweretsa anthu oiona.” 70. Iwo adati: “Pempha
kwa Ambuye wako kuti atiuze ife maonekedwe eni eni a
ng’ombeyi. Ndithudi kwa ife, ng’ombe zonse ndi zofanana.
Ngati Mulungu afuna, ife tidzalangizidwa bwino.”
71. Mose adati: “Ndithudi Ambuye wanu akuti ndi ng’ombe
imene siinaphunzitsidwe ntchito yolima m’munda kapena
yonyamula madzi othiririra m’minda, ndipo ndi ng’ombe
yopanda chilema ndi yopanda banga”. Iwo adati: “Tsono
iwe wadza ndi choona”. Ndipo iwo adapha ng’ombe
ija ngakhale anali pafupi kuti asatero. 72. Ndi pamene
mudapha munthu ndipo mudayamba kumakanirana wina
ndi mnzake. Koma Mulungu anaulula zimene mumabisa.
73. Ndipo Ife tidati: “Menya mtembo ndi mnofu wa

ng'ombe". Mmenemo ndi mmene Mulungu adzadzutsire
akufa ndipo amakulangizani zizindikiro zake kuti mukhale
ozindikira.
74. Ndipo zitatero mitima yanu idauma ngati mwala
kapena kuposerapo. Ndithudi pali miyala ina imene
imakhala magwero a mitsinje pamene ina idaphwanyika
ndipo madzi adatuluka mu iyo. Ndipo, ndithudi, ina
mwa iyo imagwa pansi chifukwa choopa Mulungu. Sikuti
Mulungu sadziwa zimene mumachita.
75. Kodi inu muli kuganiza kuti iwo adzakukhulupirirani
ngakh ale kuti gulu lina linali kumva mawu a Mulungu
ndipo anali kumawasintha pamene iwo ali kuzindikira
ndiponso iwo ali kudziwa chimenechi? 76. Ndipo
pamene iwo akumana ndi anthu okhulupirira amanena
kuti: "Nafenso timakhulupirira". Koma akakhala okha
pagulu lawo amanena wina kwa mnzake kuti: "Kodi inu
mudzawalalikira iwo zimene Mulungu wavumbulutsa kwa
inu kuti adzakutsutseni pamaso pa Ambuye wanu? Kodi
inu mulibe nzeru?" 77. Kodi iwo sadziwa kuti Mulungu
amadziwa zimene iwo amabisa ndi zimene amaziulula?
78. Ndipo pali ena mwa iwo amene ndi osaphunzira
amene sadziwa za m'Buku koma amakhulupirira mabodza
ndi zongoganizira chabe. 79. Motero tsoka kwa iwo
amene amalemba Buku ndi manja awo ndipo amanena
kuti: "Mawu awa achoka kwa Mulungu ndi kugula ndi
ilo mphatso yochepa". Tsoka kwa iwo pa zimene alemba
manja awo ndipo tsoka kwa iwo pa zimene akupeza
chifukwa cha izo. 80. Iwo adati: "Ife sitidzakhudzidwa ndi
moto kupatula masiku owerengeka okha". Nena: "Kodi inu
mwapanga lonjezo ndi Mulungu limene Iye sadzaphwanya?

Kapena kodi inu mumanena zinthu zokhudzana Mulungu zimene simuzidziwa?” 81. Inde! Yense amene achita zoipa ndipo azunguliridwa ndi machimo ake, adzakhala eni ake a Gahena. Kumeneko adzakhalako mpaka kalekale. 82. Ndipo iwo amene ali ndi chikhulupiriro ndipo amachita ntchito zabwino, iwo ndi eni ake a Paradiso ndipo adzakhala komweko mpaka kale kale.

83. Ndi pamene Ife tinamvana ndi ana a Israeli: “Musapembedze wina koma Mulungu yekha ndipo onetsani chifundo kwa makolo anu, kwa abale anu, kwa ana a masiye ndi kwa anthu ovutika, ndipo auzeni anthu kuti azichita zabwino. Pempherani pa nthawi yake ndipo perekani msonkho wothandizila anthu osauka”. Komatu inu mudabwerera m’mbuyo kupatula owerengeka okha ndipo simudalabadire china chilichonse.

84. Ndi pamene Ife tinamvana kuti: “Musakhetse magazi a anthu anu kapena kupirikitsa anthu anu kumalo amene muli kukhala”. Zimenezi inu mudavomera ndikuchitira umboni. 85. Zitatha izi ndinu amene mudayamba kupha abale anu ndi kupirikitsa gulu lina la inu m’nyumba zawo ndi kuthandiza adani awo pochita machimo ndi kuswa malamulo. Ndipo iwo akamabwera kwa inu ngati akapolo, inu muwaombola ngakhale kuti kupilikitsidwa kwawo kudali koletsedwa kwa inu. Kodi inu mukhulupirira gawo lina la Mau a Mulungu ndi kukana gawo linzake? Kodi ndi malipiro otani amene angalandire wochita zimenezo mwa inu, kupatula mphotho yochititsa manyazi m’dziko lino ndi chilango chowawa kwambiri patsiku louka kwa akufa? Mulungu saiwala ntchito zanu zimene muchita. 86. Awo ndiwo amene amagula moyo wa padziko lino lapansi

pa mtengo wa moyo umene uli nkudza. Chilango chawo
sichidzachepetsedwa ayi ndiponso sadzathandizidwa.
87. Ndithudi Ife tidamupatsa Mose Buku, ndipo iye
atachoka, Ife tidatumiza Atumwi ena. Ndipo tidamupatsa
Yesu, mwana wa Maria, zizindikiro zooneka ndi maso ndipo
tidamulimbikitsa iye ndi Mzimu Woyera. Kodi nthawi ili
yonse imene Aneneri amabwera ndi zimene mitima yanu
siifuna mumadzikweza? Gulu lina mumalikana ndipo
gulu lina mumalipha. 88. Iwo adati: "Mitima yathu ndi
yokutidwa." Iyayi, Mulungu wawatemberera chifukwa
cha kusakhupirira kwawo ndipo ndi zochepa zimene iwo
amakhulupirira.
89. Ndipo pamene Buku lidadza kwa iwo kuchokera kwa
Mulungu, kutsimikiza zimene iwo adali nazo, ngakhale
kuti kuyambira kale kale akhala ali kupempha chithandizo
kwa Mulungu choti agonjetse anthu osakhulupirira; ndipo
pamene chidadza kwa iwo, chimene iwo amadziwa, iwo
sadachikhulupirire mu icho. Motero temberero la Mulungu
likhale pa anthu osakhulupirira. 90. Ndi zoipa zomwe
asinthanitsa ndi miyoyo yawo pokana zomwe Mulungu
wavumbulutsa chifukwa cha kaduka kuti Mulungu
wavumbulutsa zabwino kwa amene Iye wamufuna
mwa akapolo ake. Iwo adziputira mkwiyo powonjezera
pamkwiyo wina. Ndipo chilango choopsa chili kuwadikira
anthu osakhulupirira.
91. Ndipo pamene adauzidwa kuti: "Khulupiririrani
mu zimene Mulungu wavumbulutsa", iwo adati: "Ife
timakhulupirira m'mawu amene adavumbulutsidwa kwa
ife." Ndipo iwo sakhulupilira zimene zavumbulutsidwa
posachedwapa ngakhale kuti ndicho choonadi, chimene

chikutsimikiza zimene ali nazo. Nena: "Nanga ndi chifukwa
chiyani inu mudali kupha Atumwi a Mulungu kale ngati,
mudali okhulupiriradi?" 92. Ndithudi Mose adadza kwa
inu ndi zizindikiro zooneka koma inu mudatenga ng'ombe
ndi kuipembedza iye atachoka ndipo inu munali ochimwa.
93. Ndi pamene tidachita pangano ndi inu Ife tidakweza
phiri kukhala pamwamba panu ndi kunena kuti: "Sungani
zonse zimene takupatsani ndipo muzimvera". Iwo adati:
"Tamva koma sitimvera". Chifukwa cha kusakhulupirira
kwawo, kupembedza ng'ombe kudakhazikika m'mitima
yawo. Nena: "Choipa ndi chimene chikhulupiriro chanu
chili kukukakamizani ngati inu ndinu okhulupirira."
94. Nena: "Ngati nyumba zamtsogolo za Mulungu ndi
zanu zokha ndipo kuti sizidzapatsidwa kwa anthu ena,
lakalakani imfa ngati zimene munena ndi zoona." 95. Koma
iwo sadzalakalaka imfa m'pang'ono pomwe chifukwa cha
zoipa zimene adatsogoza manja awo. Ndipo Mulungu
amadziwa anthu ochita zosalungama 96. Ndithudi iwe
udzawapeza kuti iwo amakonda kwambiri moyo uno
kuposa aja amene amaphatikiza Mulungu ndi zinthu zina
ndipo sakhulupirira kuti kuli kuuka kwa akufa. Aliyense wa
iwo akadakondwera ngati akadapatsidwa moyo wokwana
zaka chikwi chimodzi. Komabe ngakhale atawonjezeredwa
moyo wautali, siungamuchotsere chilango. Ndipo Mulungu
ali kuona zonse zimene ali kuchita.

97. Nena: "Aliyense amene ndi mdani wa Gabiriyeli,
chifukwa, ndithudi, iye wabweretsa chibvumbulutso mu
mtima mwako mwachifuniro cha Mulungu, kutsimikiza
zimene zidadza kale icho chisanadze ndipo ndi chilangizo
ndi nkhani yabwino kwa okhulupirira. 98. Aliyense

amene ali mdani wa Mulungu, Angelo ake, Atumwi ake,
Gabiriyeli ndi Michael, ndithudi, Mulungu ndi mdani
wa anthu osakhulupirira. 99. Ndithudi Ife tatsitsa kwa
iwe chivumbulutso chomveka bwino ndipo palibe amene
amachikana kupatula anthu ochita zoipa. 100. Kodi ndi
chizolowezi chawo choti nthawi zonse iwo akachita
pangano, ena mwa iwo amaliswa? Iyayi! Choonadi ndi
chakuti ambiri a iwo sakhulupirira. 101. Ndipo pamene
kudadza kwa iwo Mtumwi wochokera kwa Mulungu,
kutsimikiza zimene adali nazo, gulu lina la anthu amene
adapatsidwa mau a Mulungu adataya kumbuyo kwawo
Buku la Mulungu ngati kuti iwo sakulidziwa!

102. Iwo adatsatira zimene a Satana adanena mu Ufumu
wa Solomoni. Sikuti Solomoni sadakhulupirire ai koma a
Satana ndiwo sadakhulupirire. Iwo amaphunzitsa anthu
matsenga ndi zimene zidavumbulutsidwa kwa angelo awiri
Harut ndi Marut ku Babuloni. Koma iwo samaphunzitsa
wina aliyense mpaka atanena kuti: "Ndithudi ife tili
kukuyesani inu, ndipo musakhale wosakhulupirira ayi."
Kuchokera kwa angelo chimene chimamasula pakati
pa mwamuna ndi mkazi wake, ndipo iwo sadaononge
wina aliyense ndi zimene adaphunzira kupatula ndi
chilolezo cha Mulungu. Iwo amaphunzira zinthu zimene
zimawaononga ndipo sizidawapindulire china chilichonse.
Ndithudi iwo amadziwa kuti aliyense amene amachita
matsenga sadzakhala ndi gawo m'moyo umene uli nkudza.
Zopanda pake ndi zimene agulitsa nazo moyo wawo, iwo
akadadziwa. 103. Iwo akadakhulupirira ndi kudziteteza
ku zoipa, mphotho yawo yochokera kwa Ambuye wawo
ikanakhala yabwino, ngati iwo akadadziwa.

104. Oh inu anthu okhulupirira! Musanene kwa Mtumwi
wathu kuti: “Timvere ife” koma muyenera kunena
kuti mutiyang’anile ife ndipo mverani. Anthu onse
osakhulupirira ali ndi chilango chowawa. 105. Sichifuniro
cha anthu osakhulupirira amene ali pakati pa anthu
otsatira za Buku kapena anthu akunja kuti china chake
chabwino chidze kwa iwe kuchokera kwa Ambuye wako.
Koma Mulungu amasankha wina aliyense amene Iye afuna
kuti alandire chisomo chake ndipo Mulungu ndiye mwini
zabwino zazikulu. 106. Ngati Ife tisintha vesi lina kapena
tichititsa kuti liiwalike, Ife tiikamo lina labwino lolowa
m’malo mwake kapena lolingana nalo. Kodi iwe siudziwa
kuti Mulungu ali ndi mphamvu pa chilichonse? 107. Kodi
iwe siudziwa kuti ndi Mulungu amene ali Mwini ufumu
wa kumwamba ndi dziko lapansi ndipo kuti kupatula
Iye yekha kulibe wina amene akhoza kukuteteza kapena
kukuthandiza? 108. Kapena mukufuna kumufunsa Mtumwi
wanu monga mmene adamufunsira Mose kale? Ndipo
aliyense amene asintha chikhulupiriro chake ndi kuyamba
kusakhulupirira ndithudi wasochera ku njira yoyenera.

109. Anthu ambiri otsatira a m’Buku amafuna kuti
akusokeretse chifukwa cha kaduka kuti ukhale
osakhulupirira ngakhale pamene choonadi chaonekera
poyera kwa iwo. Koma akhululukire mpaka pamene
Mulungu abweretsa lamulo lake. Ndithudi Mulungu ali ndi
mphamvu pa zinthu zonse. 110. Ndipo pitiriza mapemphero
ndipo pereka msonkho wothandiza anthu osauka.
Ndipo chilichonse chabwino chimene mungatsogoze
mudzachipeza kwa Mulungu. Ndithudi Mulungu amaona
zonse zimene muli kuchita. 111. Iwo amanena kuti: “Palibe

amene adzalowa ku Paradiso kupatula yekhayo amene
ali Myuda kapena Mkhirisitu. Zimenezo ndizo zilako
lako zawo. Nena: "Bweretsani umboni wanu ngati muli
ndi chilungamo." 112. Inde aliyense amene amadzipereka
kwathunthu kwa Mulungu ndipo amachita ntchito
zabwino adzapeza malipiro ake kwa Ambuye wake. Iwo
sadzaopa china chilichonse kapena kukhumudwa.
113. Ayuda anati: Akhirisitu satsatira china chilichonse
chabwino pamene Akhirisitu anati, Ayuda satsatira
chilichonse ngakhale kuti onse amawerenga Buku la
Mulungu. Izi zili chimodzimodzi ndi zimene anthu
osazindikira amalankhula. Mulungu adzaweruza pakati
pawo tsiku la chiweruzo mu zimene adali kusiyana
maganizo awo. 114. Kodi olakwa kwambiri ndani kuposa
amene aletsa anthu kuti dzina la Mulungu lizitchulidwa mu
Mizikiti ya Mulungu ndi kulimbikitsa kuiononga? Kotero
iwo satha kulowa mu Mizikiti koma mwamantha. Iwo
adzachititsidwa manyazi m'dziko lino ndipo adzalangidwa
koposa m'dziko limene lili nkudza. 115. Mulungu ndiye Mwini
wake wa ku m'mawa ndi ku madzulo, motero mbali iliyonse
imene muyang'ana kuli Mulungu. Ndithudi Iye ndi okwana
pa zofuna za zolengedwa zake ndipo Iye amadziwa china
chilichonse. 116. Iwo amati: "Mulungu wabereka mwana."
Mulungu ayeretsedwe ku zimenezi. Zake ndi zonse zimene
zili kumwamba ndi m'dziko lapansi ndipo zinthu zonse
zimagonja kwa Iye. 117. Namalenga wa kumwamba ndi
dziko lapansi! Pamene Iye alamulira chinthu amangonena
kuti: "Chikhale" ndipo chimakhaladi.
118. Ndipo anthu osadziwa amati: "Kodi ndi chifukwa
chiyani Mulungu sakutilankhula kapena kutibweretsera

chizindikiro?” Mmenemo ndi mmene adanenera anthu amene adalipo kale iwo asadadze. Mitima yawo yonse ndi yolingana. Ndithudi Ife tafotokoza zizindikiro kwa anthu okhulupirira. 119. Ndithudi Ife takutumiza ndi choonadi kuti ulalikire uthenga wosangalatsa ndi kupereka chenjezo. Siudzafunsidwa za anthu okhala ku moto. 120. Ayuda kapena Akhirisitu sadzakondwera nawe pokhapokha ngati iwe utsatira chipembedzo chawo. Nena: “Ndithudi njira yoyenera ya Mulungu ndiyo njira yeniyeni.” Ndipo ngati iwe pamene walandira nzeru zimene wapatsidwa, utsatira zifuniro zawo, iwe siudzapeza wina aliyense wokuthandiza kapena kukuteteza ku mkwiyo wa Mulungu. 121. Kwa iwo amene tidawapatsa Buku, amaliwerenga monga momwe liyenera kuwerengedwera. Iwo amakhulupirira za bukuli, koma iwo amene amalikana ilo, ndithudi ndi olephera.

122. Oh Inu ana a Israeli! Kumbukirani madalitso anga kwa inu ndipo ndinakudalitsani inu kuposa mitundu yonse pa dziko la pansi. 123. Liopeni tsiku limene munthu sadzathandiza munthu wina pa china chilichonse ndiponso nthawi imene kupepesa kapena kupereka dipo sikudzavomerezeka ndipo iwo sadzapeza thandizo. 124. Ndi pamene Abrahamu anayesedwa ndi Ambuye wake kuti atsatire malamulo ena amene iye adakwaniritsa. Iye adati: “Ndithudi Ine ndidzakupanga iwe kukhala mtsogoleri wa mitundu ya anthu onse.” Abrahamu adapempha: “Ndi atsogoleri ochokera mwa ana anga?” Iye adati: “Pangano langa silikhudza anthu ochita zoipa.”

125. Ndi pamene tidaipanga Nyumba kukhala malo opumuliramo ndi obisalamo anthu: Dzisankhireni malo amene Abrahamu adaimapo, ngati malo opempheramo.

Ife tidamulamula Abrahamu ndi Ishimayeli kuti "ayeretse
nyumba yanga" kuti anthu amene amayenda moizungulira
kapena amaigwiritsa ntchito ngati malo obindikiramo ndi
mtima onse kapena malo wolambiramo pamene ali mkati
mwa mapemphero. 126. Ndi pamene Abrahamu adati:
"Ambuye wanga upangeni Mzinda uno kukhala Mzinda wa
mtendere ndipo muwapatse zipatso zambiri anthu ake, iwo
amene amakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza."
Iye adati: "Inde koma iye amene akana kukhulupirira,
Ine ndidzamusangalatsa mwa kanthawi kochepa koma
ndidzamududuluza kupita ku chilango cha ku Gahena,
malo oipa zedi kukhalako."
127. Ndi pamene Abrahamu ndi Ishimayeli adamanga
maziko a Nyumba. Anati: Ambuye wathu; Landirani ichi
kuchokera kwa ife. Ndithudi inu mumamva zonse ndipo
mumadziwa chinthu china chilichonse." 128. "Ambuye wathu!
Tipangeni ife kukhala okumverani Inu ndi ana athu kukhala
mtundu umene udzakumverani Inu ndipo tiphunzitseni
miyambo yathu yopembedzera ndipo mutikhululukire.
Ndithudi Inu ndinu okhululukira ndi Wachisoni chosatha."
129. "Oh Ambuye wathu! Atumizireni Mtumwi kuchokera
kumtundu wawo amene adzawawerengera Mawu Anu ndi
kuwaphunzitsa Buku ndiponso luntha ndi kuwayeretsa iwo
ku machimo awo. Ndithudi Inu ndinu Mwini mphamvu
zonse ndi Mwini nzeru zonse."
130. Ndani, kupatula munthu wopusa yekha, amene
angaleke kutsatira chikhulupiriro cha Abrahamu? Ndithudi
Ife tidamusankha iye m'dziko lino ndipo, ndithudi, m'dziko
limene lili nkudza, iye adzakhala pamodzi ndi anthu
olungama. 131. Pamene Ambuye wake adati: "Dzipereke,"

iye adati: “Ine ndadzipereka kwa Ambuye wa zolengedwa
zonse.” 132. Abrahamu analangiza chikhulupiriro chake pa
ana ake ndi Yakobo. “Oh ana anga! Ndithudi Mulungu
wakusankhirani inu chipembedzo ndipo musamwalire
ngati anthu wamba ai koma ngati Asilamu.” 133. Kodi kapena
inu mudalipo pamene Yakobo imamufikira imfa? Pamene
adawauza ana ake kuti: “Kodi inu mudzapembedza ndani
pambuyo panga?” Iwo adati: “Ife tidzapembedza Mulungu
wanu ndi Mulungu wa makolo anu Abrahamu, Ishimayeli
ndi Isake, Mulungu mmodzi yekha. Ndipo kwa Iye, ife
tidzadzipereka ngati Asilamu.” 134. Umenewu ndi mbadwo
umene udafa kale. Iwo adzalandira zimene adachita ndipo
inu mudzalandira mphoto ya zimene muchita. Ndipo inu
simudzafunsidwa zimene iwo amachita.

135. Iwo adati: “Khalani Ayuda kapena Akhirisitu ndipo
mudzatsogozedwa ku choonadi.” Nenani: “Iyayi! Koma
Chipembedzo cha Abrahamu wangwiro, ndipo iye sanali
kupembedza mafano.” 136. Nenani: “Ife timakhulupirira mwa
Mulungu ndi zimene zavumbulutsidwa kwa ife, ndi zimene
zinavumbulutsidwa kwa Abrahamu, Ishimayeli, Isake,
Yakobo ndi kwa mitundu ya anthu ndi zimene adapatsidwa
Mose ndi Yesu ndi zimene adapatsidwa Atumwi ena
kuchokera kwa Ambuye wawo. Ife sitisiyanitsa pakati pa
aliyense wa iwo ndipo ndi kwa Iye kumene tadzipereka
kwathunthu.” 137. Ndipo ngati iwo akhulupirira monga
mmene mwakhulupirira inu ndiye kuti ndi olangizidwa
bwino, koma ngati akana, ndithudi iwo ndi otsutsa
chabe. Polimbana ndi iwo, Mulungu adzakuteteza. Iye
amamva zonse ndipo amadziwa chinthu china chilichonse.
138. Chipembedzo chathu ndi chochokera kwa Mulungu.

Kodi chipembedzo chabwino kuposa cha Mulungu ndi chiti? Ndipo ife ndife timamupembedza Iye. 139. Nena: "Kodi mukutsutsana ndi ife pa nkhani zokhudza Mulungu amene ali Ambuye wathu ndi Ambuye wanu? Ife tili ndi udindo pa ntchito zathu, nanu pa ntchito zanu. Ndi kwa Iye yekha kumene ife tadzipereka." 140. Kodi kapena inu mukunena kuti Abrahamu, Ishimayeli, Isake, Yakobo ndi mitundu yake adali Ayuda kapena Akhirisitu? Nena: "Kodi inu mumadziwa kapena Mulungu? Kodi oipa kwambiri ndani kuposa munthu amene amabisa mawu amene walandira kuchokera kwa Mulungu? Koma Mulungu saiwala zimene mukuchita." 141. Umenewo ndi mbadwo umene udafa kale. Iwo adzalandira mphotho ya zimene adachita ndipo inu mudzalandira ya zimene mumachita. Ndipo inu simudzafunsidwa zimene iwo amachita.

142. Anthu opusa adzanena: "Kodi ndi chifukwa chiyani asintha malo oyang'anako akamapemphera?" Nena: "Mwini wake wa ku m'mawa ndi ku madzulo ndi Mulungu. Iye amatsogolera yemwe wamufuna ku njira yoyenera." 143. Motero Ife takupangani inu kukhala mtundu wa anthu angwiro kuti mukhale mboni kwa anthu ndi kuti Mtumwi akhale mboni kwa inu. Ndipo Ife tidakhazikitsa mbali imene unkayang'anako kale ndi cholinga choona anthu amene amatsatira Mtumwi ndi iwo amene amabwerera m'mbuyo. Ndithudi uwu ndi muyeso waukulu kupatula kwa iwo amene adatsogozedwa ndi Mulungu. Ndipo Mulungu sakanapanga chikhulupiriro chanu kuti chikhale chopanda phindu. Ndithudi Mulungu ali ndi chifundo chambiri ndi chisoni kwa anthu.

144. Ndithudi nthawi zambiri Ife takhala tili kukuona

uli kuyang'ana kumwamba. Ndithudi Ife tidzakulamula kuti uziyang'ana ku mbali yimene idzakukondweretsa iwe, motero yang'anitsa nkhope yako kumene kuli Mzikiti Woyera ndipo kuli konse kumene muli yang'anani nkhope zanu komweko. Ndithudi iwo amene adapatsidwa Buku kale amadziwa kuti ichi ndi choonadi chochokera kwa Ambuye wawo. Ndipo Mulungu saiwala zomwe muchita.
145. Ngakhale kuti iwe utawapatsa umboni wotsimikiza, iwo amene anapatsidwa Buku, sadzayang'ana kumalo kumene uli kuyang'ana ukamapemphera. Ndipo iwe siudzayang'ana ku mbali kwawo. Ndipo iwo sadzayang'ana ku mbali ya anzawo. Ndipo ngati, pamene nzeru zapatsidwa kwa iwe, uvomeleza zilakolako zawo, ndithudi iwe udzakhala munthu wolakwa kwambiri. 146. Iwo amene tidawapatsa Buku, amamuzindikira Mtumwi monga momwe amazindikirira ana awo amuna. Koma, ndithudi, ena mwa iwo amabisa choonadi pamene iwo ali kudziwa.
147. Ndi choonadi chochokera kwa Ambuye wako. Motero usachikaikire ayi.

148. Mtundu uli wonse uli ndi mbali imene umayang'ana popemphera. Motero limbikirani pochita zabwino. Kulikonse kumene mudzakhale, Mulungu adzakusonkhanitsani pamodzi. Ndithudi Mulungu ali ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse. 149. Ndipo dera lililonse limene uchokera, yang'ana nkhope yako ku Mzikiti Woyera popemphera, chifukwa chimenechi ndicho choonadi chochokera kwa Ambuye wako. Ndipo Mulungu saiwala zomwe mumachita. 150. Ndipo dera lililonse limene uchokera, yang'ana nkhope yako ku Mzikiti Woyera popemphera. Kulikonse kumene mungakhale, yang'anani

nkhope zanu komweko kuti anthu asakhale ndi nkhani
yokudzudzulani inu kupatula okhawo amene ndi olakwa.
Motero musawaope iwo koma opani Ine kuti ndikwaniritse
madalitso anga pa inu ndiponso kuti mukhale otsogozedwa.
151. Monga takutumizirani Mtumwi kuchokera ku mtundu
wanu, kuti akuwerengereni chivumbulutso chathu ndi
kukuyeretsani machimo ndiponso kukuphunzitsani inu za
Buku ndi nzeru zakuya ndiponso akuphunzitseni zinthu
zimene simudali kuzidziwa. 152. Motero ndikumbukireni
Ine. Ndipo Ine ndidzakukumbukirani inu ndipo
ndiyamikeni Ine ndipo musakhale wosathokoza.

153. Oh Inu anthu okhulupirira! Funani chithandizo
popirira ndi popemphera. Ndithudi! Mulungu ali pamodzi
ndi anthu opirira. 154. Ndipo musanene za iwo amene
aphedwa mu njira ya Mulungu kuti ndi akufa ayi, chifukwa
iwo ali ndi moyo koma inu simudziwa. 155. Ndipo, ndithudi,
Ife tidzakuyesani ndi mantha ndi njala ndi kuchepetsa
chuma chanu, moyo wanu ndi zipatso, koma auzeni nkhani
yabwino iwo amene amapirira kwambiri. 156. Amene amati
akapeza mavuto, amanena kuti: "Ndithudi! Ambuye wathu
ndi Mulungu ndipo ndi kwa Iye kumene tidzabwerera."
157. Iwo ndiwo adzalandira madalitso ndi chisoni chochokera
kwa Ambuye wawo, ndipo ndiwo amene ali otsogozedwa
kwenikweni.

158. Ndithudi! Swafa ndi Marwa ndi zizindikiro za
Mulungu kwa amene amabwera kudzachita mapemphero
ku Nyumba ya Mulungu. Palibe cholakwa kwa amene
achita Hajji kapena Umra ngati azungulira pa malo awiriwa.
Ndipo kwa amene achita chabwino mosakakamizidwa,
ndithudi, Mulungu ndi wosangalala ndipo ndi wozindikira.

159. Ndithudi iwo amene amabisa umboni wooneka ndi
ulangizi umene tidatumiza Ife titaululа kwa anthu a m'Buku,
iwo ndiwo otembereredwa ndi Mulungu ndi iwo omwe ali
ndi mphamvu yotemberera. 160. Kupatula okhawo, amene
alapa machimo awo ndi kumachita ntchito zabwino ndipo
aulula poyera. Awa ndiwo amene ndidzawakhululukira.
Ndipo Ine ndine wokhululukira ndi Mwini chisoni
chosatha. 161. Ndithudi iwo amene sakhulupirira ndipo
afa ali osakhulupirira, ndi pa iwo pamene pali temberero
la Mulungu, temberero la angelo ndiponso la anthu onse.
162. Iwo adzakhalamo mpaka kalekale, ndipo chilango
chawo sichidzachepetsedwa ayi ndiponso sadzapatsidwa
nthawi yopuma.

163. Mulungu wanu ndi Mulungu m'modzi yekha.
Kulibenso wina wopembedzedwa muchoonadi koma
Iye yekha. Iye ndi Mwini chifundo ndi chisoni chosatha.
164. Ndithudi! Muchilengedwe chakumwamba ndi dziko
lapansi ndiponso mukasinthidwe ka usiku ndi usana,
ndi m'zombo zimene zimayenda pa nyanja zitanyamula
katundu wothandiza anthu, ndi mvula imene Mulungu
amagwetsa kuchokera ku mitambo ndipo imaukitsa
nthaka imene idali yakufa, ndi mayendedwe a nyama
zosiyanasiyana zimene Iye amazimwanza pa dziko lapansi;
ndiponso mphepo ndi mitambo imene imakhala pakati pa
kumwamba ndi dziko lapansi, ndithudi mu zimenezi muli
zizindikiro kwa anthu anzeru.

165. Ndipo pakati pawo pali anthu amene amapembedza
milungu ina m'malo mwa Mulungu weniweni. Iwo
amaikonda iyo monga momwe amkondera Mulungu.
Koma iwo amene ali okhulupirira amakhala ndi chikondi

chosefukira pa Mulungu. Ngati anthu osakhulupirira
akadaona, pamene iwo adzaona chilango chawo akadadziwa
kuti Mulungu ndiye mwini mphamvu ndi kuti Mulungu
amapereka chilango chowawa. 166. Pamene iwo amene anali
kutsatiridwa adzawakana iwo amene adali kuwatsatira,
ndi kuona chilango, ubale wonse umene unali pakati
pawo udzatha. 167. Ndipo iwo amene adali kuwatsatira
adzati: "Kukanakhala kuti tikadatha kubwereranso, Ife
tikadawakana monga momwe atikanira ife tsopano."
Motero Mulungu adzawaonetsa ntchito zawo kukhala
zinthu zopanda pake. Ndipo sipadzakhala njira yothawira
ku moto.

168. Oh Inu anthu! Idyani zinthu zabwino zimene
mwaloledwa kudya pa dziko lapansi ndipo musatsatire
mapazi a Satana chifukwa iye ndi mdani wanu weniweni.
169. Iye amakulamulirani kuti muzichita zoipa ndi
zonyansa ndi kuti muzinena zokhudza Mulungu zimene
inu simuzidziwa. 170. Ndipo pamene zimanenedwa kwa
iwo kuti: Tsatirani zimene Mulungu wavumbulutsa, iwo
amayankha: "Iyayi, ife tidzatsatira zimene tidapeza makolo
athu ali kuchita." Ngakhale kuti makolo awo adali osadziwa
kapena osowa chilangizo.? 171. Ndipo fanizo la anthu
osakhulupirira lili ngati la iye amene aitana zinthu zimene
sizizindikira china chilichonse koma kuitanidwa ndi kulira.
Osamva, osalankhula ndi akhungu, iwo sazindikira china
chilichonse.

172. Oh inu anthu okhulupirira! Idyani zinthu zabwino
zimene takupatsani inu ndipo thokozani Mulungu ngati
Iye ndiye amene inu mumampembedza. 173. Iye wakuletsani
kudya nyama yofa yokha, liwende ndi nyama ya nkhumba,

ndiponso nyama ina iliyonse imene yaphedwa ngati nsembe m'dzina lina lililonse kupatula dzina la Mulungu. Koma aliyense amene wapanikizidwa kudya zina za izi, osati ndi cholinga choipa kapena kuswa malamulo, iye sali olakwa ayi. Mulungu ndi wokhululukira ndiponso ndi Wachisoni.
174. Ndithudi iwo amene amabisa chivumbulutso cha Mulungu chimene chili m'Buku ndipo amagula phindu lochepa ndi icho, sameza m'mimba mwawo china chilichonse koma moto. Mulungu sadzalankhula nawo pa tsiku louka kwa akufa kapena kuwayeretsa. Chawo chidzakhala chilango chowawa.
175. Amenewa ndiwo amene agula chinthu choipa pa mtengo wa chilangizo chabwino ndi chilango pa mtengo wa chikhululukiriro. Iwo ndi wodzipereka ku moto.
176. Ichi ndi chifukwa chakuti Mulungu adatumiza Buku mwa choonadi. Ndithudi iwo amene amatsutsa zimene zili m'Buku ali kutali ndi chilungamo.

177. Chilungamo sichili m'machitidwe oti muziyang'ana ku m'mawa kapena ku madzulo, koma chilungamo ndi kukhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza, mwa angelo ndi Buku la Mulungu, mwa Atumwi ndiponso kupereka chuma chimene amachikonda kwa abale ake, kwa a masiye, kwa anthu osauka, kwa a paulendo, kwa anthu opempha ndi kuombola a kapolo. Ndipo onse amene amasamala mapemphero ndipo amapereka msonkho wothandiza anthu osauka ndi amene amakwaniritsa lonjezo lawo akalonjeza ndipo amakhala opirira pa mayesero ndi m'mavuto ndiponso m'nthawi za nkhondo, amenewa ndiwo okhulupirira enieni ndiponso amenewa ndiwo amene amaopa Mulungu.

178. Oh inu anthu okhulupirira! Kubwezera ndi kololedwa
kwa inu pa nkhani zokhudza kukhetsa mwazi. Mfulu kwa
mfulu, kapolo kwa kapolo, mkazi kwa mkazi. Aliyense
amene akhululukidwa ndi m'bale wa ophedwa chiweruzo
chake chikhale choyenera polipira ndipo alipire kwa iwo
wofedwa mwaubwino. Umenewu ndi mwambo wachifundo
wochokera kwa Ambuye wanu. Aliyense amene adzalumpha
malire pambuyo pake, adzakhala ndi chilango chowawa.
179. Muli moyo mu kubwezera, Oh inu anthu ozindikira!
180. Mwalamulidwa kuti ngati imfa idza kwa mmodzi wa inu,
ngati iye asiya chuma chake, kuti asiye mawu ofotokoza
kagawidwe ka chuma chake mwachilungamo kwa makolo
ndi achibale ake. Uwu ndi udindo wokhazikitsidwa kwa
anthu olungama. 181. Ndipo yense amene adzasintha
mawu osiyidwa ndi munthu wakufa, uchimo udzakhala
pa munthu osinthayo. Ndithudi Mulungu ndi Wakumva
ndi Wozindikira. 182. Koma iye amene aopa kuti munthu
wochitira umboni akhoza kukondera kapena kulakwa
ndipo abweretsa chiweruzo chabwino pakati pa anthu
otsutsana, iye sali wolakwa pa china chilichonse. Ndithudi
Mulungu ndi wokhululukira ndi wachisoni chosatha.

183. Oh inu anthu okhulupirira! Kusala kudalamulidwa
kwa inu monga momwe kudalamulidwa kwa iwo amene
adalipo kalero inu musanadze kuti inu mukhale woyera.
184. M'masiku owerengeka, koma ngati wina wa inu ndi
wodwala kapena ali pa ulendo, awerengere kuti adzasale
masiku ena olingana ndi amene sadasale. Ndipo iwo amene
sangathe, apereke nsembe yodyetsa munthu wosauka.
Koma wina aliyense amene amachita chabwino mwayekha
adzalipidwa ndi manja awiri. Koma ngati inu musala

chimenecho ndicho chinthu chabwino kwa inu ngati inu
mukadadziwa. 185. M'mwezi wa Ramazani ndi mmene
Korani idavumbulutsidwa. Iyo ndi ulangizi kwa anthu
ndi umboni wooneka wolangiza ndi kusiyanitsa. Motero
aliyense wa inu amene wauona mwezi umenewu, ayenera
kusala. Koma yense amene ali kudwala kapena ali paulendo,
adzasale masiku ofanana ndi amene sadasale. Mulungu
akufuna kukupeputsirani zinthu osati kuonjeza masautso
ayi. (Iye) afuna kuti mukwaniritse kusala masiku onse
olamulidwa ndiponso muyenera kumalemekeza Mulungu
chifukwa chokutsogolerani kuti mukhale othokoza.
186. Ndipo pamene akapolo anga akufunsa za Ine, auze
kuti: "Ndithudi Ine ndili pafupi ndipo ndimayankha
pempho la aliyense akandipempha. Motero andimvere Ine
ndi kukhulupirira kuti akhoza kuyenda m'njira yoyenera.
187. Ndikololedwa kwa inu kugona ndi akazi anu mu
usiku wa kusala. Iwo ndi chofunda chanu pamene nanu
ndi chofunda chawo. Mulungu amadziwa kuti munali
kudzinyenga nokha pogona nawo opanda chilolezo. Iye
adavomera kulapa kwanu ndipo adakukhululukirani.
Tsopano mukhoza kugona nawo ndipo funani zimene
Mulungu wakulamulirani inu. Idyani ndi kumwa mpaka
pamene mukhoza kusiyanitsa pakati pa ulusi woyera ndi
wakuda pamene kuli nkucha. Ndipo pitirizani kusala
mpaka pamene dzuwa lilowa ndipo musawakhudze akazi
anu pamene muli kubindikira m'mapemphero. Amenewa
ndi malire a Mulungu ndipo musawayandikire ayi. Motero
Mulungu amafotokoza chivumbulutso chake kwa anthu
kuti akhale omuopa Iye. 188. Musadyerane chuma chanu
pakati panu mu njira yosalungama kapena kupereka

chiphuphu kwa anthu oweruza ndi cholinga chakuti
mudye chuma cha anthu ena mosalungama pamene inu
muli nkudziwa.
189. Iwo akukufunsani za miyezi yatsopano. Nena:
"Zimenezi ndi zizindikiro za nyengo kwa anthu ndi
nthawi ya Hajji. Ndipo sichilungamo kulowa m'nyumba
podzera ku khomo la kumbuyo. Koma chilungamo ndi
kuopa Mulungu. Motero lowani m'nyumba zanu kudzera
m'makomo oyenera, ndipo opani Mulungu kuti mukhale
opambana." 190. Menyanani nawo mu njira ya Mulungu, iwo
amene amenyana nanu koma musapyole malire. Ndithudi
Mulungu sakonda anthu oswa malamulo. 191. Ndipo
muwaphe paliponse pamene muwapeza, ndipo achotseni
m'malo monse m'mene adakuchotsani inu. Kusakhulupilira
ndi kupembedza mafano ndi koipa kuposa kupha. Koma
musamenyane nawo pa Mzikiti Woyera pokhapokha
atakuputani. Koma ngati iwo akuputani, muwaphe.
Imeneyo ndiyo mphotho ya anthu amene amakana
choonadi. 192. Koma ngati iwo asiya, ndithudi Mulungu ndi
Okhululuka ndi Wachisoni chosatha. 193. Menyanani nawo
mpaka pamene kusakhulupilira ndi kupembedza mafano
kutha ndiponso chipembedzo chikhala cha Mulungu
yekha. Koma ngati iwo asiya, pasakhale chidani kupatula
ndi anthu ochita zoipa.
194. Mwezi Woyera ndi Mwezi Woyera ndipo zinthu
zosaloledwa nazonso zimabwezeredwa. Ndipo aliyense
amene akuputani mubwezereni molingana ndi mmene
wachitira iye. Ndipo muopeni Mulungu ndipo dziwani
kuti Mulungu ali pamodzi ndi iwo amene amalewa zoipa.
195. Ndipo perekani m'njira ya Mulungu ndipo musadziponye

nokha kuchionongeko. Chitani zabwino. Ndithudi Mulungu amakonda anthu ochita zabwino.

196. Kwaniritsani miyambo ya Hajji ndi Umra chifukwa cha Mulungu. Ndipo ngati mwatsekerezedwa, iphani, ngati nsembe, nyama zimene sizili zovuta kuzipeza ndipo musamete mitu yanu mpaka nyama zitafika pa malo ake ophera. Koma aliyense wa inu amene ndi wodwala kapena ali ndi vuto m'mutu mwake ayenera kudziombola posala kapena kupereka nsembe kapena kupha nyama. Ngati muli pa mtendere ndiponso wina wa inu aphatikiza Umra ndi Hajji, ayenera kupha nyama imene angaipeze mosavutikira kwambiri. Koma ngati sangathe kuipeza ayenera kusala masiku atatu pa nthawi ya Hajji ndi masiku asanu ndi awiri akabwerera kwawo; amenewo ndi masiku khumi okwana. Zimenezi ndi za iye amene banja lake silili pafupi ndi Mzikiti Woyera. Muopeni Mulungu. Ndipo dziwani kuti
Mulungu amakhwimitsa chilango. 197. Nthawi ya Hajji ili
ndi miyezi yake yodziwika. Aliyense amene afuna kupanga Hajji m'menemu sayenera kugona ndi mkazi wake kapena kuchita zoipa kapena kukangana ndi anzake nthawi ya Hajji. Ndipo chabwino chilichonse chimene muchita, Mulungu amachidziwa. Mutenge kamba wa paulendo, koma kamba wabwino ndi kuopa Mulungu. Motero ndiopeni Ine, inu anthu ozindikira!

198. Palibe mlandu kwa inu ngati inu mufuna zabwino kuchokera kwa Ambuye wanu. Motero pamene muchoka ku Arafat, kumbukirani Mulungu pafupi ndi chizindikiro choyera. Ndipo mukumbukeni Iye chifukwa Iye wakutsogolerani, popeza kale ndithudi inu mudali wa
iwo amene adasokera. 199. Ndipo pitani kumalo kumene

anthu onse amapitako ndipo pemphani chikhululukiro cha Mulungu. Ndithudi Iye ndi wokhululukira ndi Wachisoni chosatha. 200. Ndipo pamene inu mukwaniritsa mapemphero anu a Hajji, kumbukirani Mulungu monga momwe mumakumbukira makolo anu kapena kuposa pamenepo. Ndipo pakati pawo pali iye amene amanena kuti: "Ambuye wathu! Tipatseni zabwino m'dziko lapansi!" Ndipo munthu wotere sadzakhala ndi gawo m'moyo umene uli nkudza. 201. Ndipo pakati pawo alipo wina wa iwo amene amati: "Ambuye wathu! Tipatseni zabwino m'dziko lino ndiponso zabwino m'dziko limene lili nkudza ndipo titetezeni ku chilango cha moto." 202. Iwo adzakhala ndi gawo chifukwa cha ntchito zomwe amachita. Mulungu ndi wachangu powerengera. 203. Ndipo kumbukira Mulungu m'masiku owerengeka. Koma iye amene afulumira kuchoka pa masiku awiri salakwa ayi ndiponso naye amene amachedwerapo salakwa ayi ngati cholinga chake ndi kuchita zabwino ndi kumvera Mulungu. Ndipo dziwani kuti nonse, ndithudi, mudzasonkhanitsidwa kunka kwa Iye.

204. Pakati pa anthu pali wina amene zolankhula zake zokhudza moyo uno zimakukondweretsa ndipo iye amaitana Mulungu kuti achitire umboni pa zimene zili mumtima mwake pamene iye ndiye wolongolola pa gulu la adani onse. 205. Ndipo pamene iye achoka, amapita uku ndi uku kuyambitsa chisokonezo m'dziko ndi kuononga mbeu ndi ng'ombe ndipo Mulungu sakonda chisokonezo. 206. Ndipo zikanenedwa kwa iye kuti: "Opa Mulungu," kudzitukumula kwake kumamupangitsa kuchita zoipa. Motero Gahena ndi yomuyenera. Ndipo ndi malo oipa

kupumirako. 207. Ndipo pakati pawo pali munthu amene amadzipereka ndi cholinga chofuna chisangalalo cha Mulungu. Ndipo Mulungu ndi odzadza ndi chifundo kwa akapolo ake.

208. Oh Inu anthu okhulupirira! Lowani Chisilamu ndi mtima wanu wonse ndipo musayende m'mapazi a Satana. Ndithudi iye ndiye mdani wanu weniweni. 209. Ndipo ngati inu muterera ndi kubwerera m'mbuyo pamene zizindikiro zadza kwa inu, dziwani kuti Mulungu ndi wa Mphamvu ndi Wanzeru. 210. Kodi iwo ali kudikira china chake kupatula kuti Mulungu awabwerere mu mthunzi wa mitambo pamodzi ndi angelo pa zomwe zatsimikizidwa ndipo zonse zimabwezedwa kwa Mulungu? 211. Afunse ana a Israeli kuti kodi ndi zizindikiro zingati zooneka zimene tidawapatsa? Ndipo aliyense amene asintha madalitso a Mulungu atawalandira, ndithudi, Mulungu ndi wokhwimitsa chilango. 212. Moyo wa pa dziko lino lapansi ndi wosangalatsa kwa anthu osakhulupirira ndipo iwo amanyogodola anthu okhulupirira. Koma iwo amene amamvera malamulo a Mulungu ndipo amalewa zoipa adzakhala wopambana pa tsiku la kuuka kwa akufa. Mulungu amapereka mopanda muyeso kwa aliyense amene Iye wamufuna.

213. Anthu onse anali mtundu umodzi ndipo Mulungu adatumiza Atumwi kudzawauza nkhani yabwino ndi kuwachenjeza ndipo ndi iwo adatumiza mau ake mwa choonadi kuti aweruze pa mikangano imene ili pakati pawo. Ndipo okhawo amene adaperekedwa amatsutsa za ilo iwo atalandira zizindikiro zooneka chifukwa cha udani wa wina ndi mzake. Ndipo Mulungu analangiza mwa chifuniro chake iwo amene amakhulupirira

m'choonadi chimene chinali kutsutsidwa. Ndipo Mulungu amatsogolera wina aliyense amene wamufuna ku njira yoyenera. 214. Kapena inu mumaganiza kuti mukalowa ku Paradiso popanda kuyesedwa monga momwe anthu amene analipo kale anaona? Iwo anapeza mavuto ndi masautso ochuluka ndipo anada nkhawa moti Mtumwi pamodzi ndi iwo amene adakhulupirira ndi iye adati: "Kodi chithandizo cha Mulungu chidzadza liti? Inde! Ndithudi, chithandizo cha Mulungu tsopano chili pafupi."

215. Iwo akukufunsa iwe kuti apeleke chiani. Nena: "Chilichonse chabwino chimene mupeleka chiyenera kuperekedwa kwa makolo anu ndi kwa abale anu, kwa ana a masiye, ndi kwa anthu osauka ndi alendo. Ndipo zabwino zilizonse zimene muchita, ndithudi Mulungu amazidziwa." 216. Nkhondo yalamulidwa kwa inu ngakhale inu simuikonda ndipo mwina inu mukhoza kudana ndi chinthu chimene chili chabwino kwa inu ndipo kuti inu mumakonda chinthu chimene chili choipa kwa inu. Mulungu amadziwa koma inu simudziwa.

217. Iwo akukufunsa zomenya nkhondo M'mwezi Woyera. Nena: "Kumenya nkhondo m'mwezi uwu ndi kulakwa kwakukulu koma kulakwa kwakukulu zedi pamaso pa Mulungu ndi kutsekereza anthu kuti atsatire njira ya Mulungu, kumukana Iye ndi kuletsa anthu kulowa mu Mzikiti Woyera ndi kupirikitsa anthu ake opembedza m'menemo. Ndipo kuchita zinthu zosokoneza chipembedzo ndi koipa kwambiri kuposa kupha munthu." Ndipo iwo sadzasiya kumenyana nanu mpaka atakuchotsani mchipembedzo chanu ngati angathe kutero. Ndipo aliyense wa inu amene adzasiye chipembedzo chake

chenicheni ndipo afa ali osakhulupirira, ntchito zake zonse zidzakhala zopanda pake m'dziko lino ndiponso m'dziko limene lili nkudza. Anthu otere adzakhala eni ake a ku Gahena ndipo kumeneko adzakhalako mpaka kalekale.
218. Ndithudi iwo amene akhulupirira ndi iwo amene adasamuka ndi kumenya nkhondo mnjira ya Mulungu, onsewa ali ndi chiyembekezo chachifundo cha Mulungu. Ndipo Mulungu ndi wokhululukira ndi Mwini chisoni chosatha.

219. Iwo akukufunsa za mowa ndi masewera a mwayi. Nena: "Mu zonsezi muli zoipa zambiri ndi zabwino kwa anthu ena. Koma zoipa zake ndi zambiri kuposa zabwino." Ndipo akukufunsa chimene angapereke. Nena: "Chilichonse chimene ndi chapadera. Mmenemo Mulungu akulangizira poyera chivumbulutso chake kuti inu mukhoza kuganizira bwino." 220. Mu za m'moyo wa m'dziko lino ndi m'moyo umene uli nkudza. Ndipo iwo akukufunsa za ana amasiye. Nena: Kuchita chilungamo kwa iwo ndi kwabwino ndipo ngati inu mukhalira pamodzi ndiye kuti, iwo ndi abale anu. Ndipo Mulungu amadziwa amene amachita zoipa ndi amene amachita zabwino, ndipo ngati Mulungu akadafuna akadakupatsani mavuto; Ndithudi Mulungu ndi wamphamvu ndi Wanzeru.

221. Musakwatire akazi opembedza mafano mpaka atakhulupirira. Ndipo, ndithudi, kapolo wachikazi wokhulupirira ali bwino kuposa mfulu yaikazi yopembedza mafano ngakhale atakukondweretsani. Ndiponso musadzakwatitse aliyense wopembedza mafano mpaka atakhulupirira. Ndithudi kapolo wokhulupirira ali bwino kuposa mfulu yopembedza mafano ngakhale kuti iye

wakusangalatsani. Iwo amakuitanirani ku moto pamene
Mulungu amakuitanirani ku Paradiso ndi ku chikhululukiro
mwachifuniro chake, ndipo Iye amafotokoza bwino bwino
chivumbulutso chake kwa anthu kuti mwina akhoza
kukumbukira. 222. Ndipo iwo akukufunsa za msambo.
Nena: "Uwu ndi umve. Motero aleweni akazi panthawi
ya msambo ndipo musawakhudze mpaka atayeretsedwa.
Ndipo akayeretsedwa, mukhoza kukhala nawo malo
amodzi monga momwe Mulungu adakulamulirani.
Ndithudi Mulungu amakonda iwo amene amadza ndi
kulapa kwa Iye. Ndipo Iye amakonda iwo wodziyeretsa."
223. Akazi anu ndi minda yanu kotero lowani m'minda yanu
monga momwe mufunira, dzitsogozereni nokha ntchito
zabwino. Ndipo muopeni Mulungu, ndipo dziwani kuti
mudzakumana naye. Ndipo pelekani nkhani yabwino kwa
anthu okhulupirira.

224. Musalipange dzina la Mulungu kukhala chida
chonamizira wina ndi mzake pa malonjezo anu polumbira
ndi kusiya kuchita zabwino ndi kuopa kukhazikitsa
mtendere pakati pa anthu. Mulungu amamva ndipo
amadziwa. 225. Mulungu sadzakulangani chifukwa cha
kuphwanya mwangozi malonjezo anu amene mudachita.
Koma adzakulangani pa zinthu zimene mitima yanu
yachita ndipo Mulungu ndi wokhululukira ndi wopirira
kwambiri. 226. Iwo amene amalumbira kuti sadzakhala malo
amodzi ndi akazi awo adikire miyezi inayi, ndipo ngati
iwo abwererana, ndithudi, Mulungu ndi wokhululukira
ndi wachifundo chosatha. 227. Ndipo ngati atsimikiza
zowasudzula, pamenepo Mulungu amamva ndipo
amadziwa zonse. 228. Ndipo akazi osudzulidwa asakwatiwe

mpaka atasamba miyezi itatu. Ndipo ndikosaloledwa kwa iwo, kubisa zimene Mulungu walenga m'mimba mwawo ngati iwo amakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza. Ndipo amuna awo akhoza kuwatenganso ngati iwo atafuna kuyanjana: Ndipo akazi adzakhala ndi mwayi wolingana ndi umene uli ndi amuna koma amuna ndi a udindo kuposa akazi. Mulungu ndi Wamphamvu ndi Wanzeru.

229. Chisudzulo ndi chololedwa kawiri kokha ndipo pambuyo pake, mukhoza kukhala naye limodzi mogwirizana kapena kusiyana mwaulemu. Ndi choletsedwa kwa inu amuna kutenga katundu wina aliyense amene mudawapatsa akazi anu pokhapokha ngati onse awiri aopa kuti sadzatha kukwaniritsa malamulo a Mulungu. Ndipo ngati inu muopa kuti iwo sadzakwaniritsa malamulo a Mulungu, palibe mlandu kwa iwo ngati mkazi apereka mphatso kapena gawo lake ngati chodziombolera. Awa ndi malamulo a Mulungu ndipo musawaswe. Ndipo aliyense amene aswa malamulo amene anakhazikitsa Mulungu, wotere ndiwo olakwa.
230. Ngati munthu asudzula mkazi wake kachitatu, iye saloledwa kumukwatiranso pokhapokha ngati atakwatiwa ndi mwamuna wina ndipo mwamunayo amusudzulanso. Sicholakwa kwa iwo kubwererana, ngati iwo atsimikiza kuti adzasunga malamulo a Mulungu. Amenewa ndi malamulo a Mulungu amene akuwaonetsa poyera kwa anthu ozindikira.
231. Ndipo pamene musudzula akazi ndipo iwo akwanitsa nthawi yawo yodikira, asungeni mwaubwino kapena alekeni mwa mtendere. Koma musawasunge ndi cholinga chowazunza. Ndipo aliyense amene achita ichi, ndithudi adzilakwira yekha. Ndipo musachite chipongwe Mau a Mulungu koma kumbukirani madalitso a Mulungu kwa inu

ndi zimene Iye watumiza m’Buku ndi luntha limene Iye
akulangizani inu. Muopeni Mulungu ndipo dziwani kuti
Mulungu amadziwa chilichonse.
232. Ndipo ngati inu musudzula akazi ndipo iwo akwanitsa
nthawi yawo yodikira, musawaletse kukwatiwa ndi amuna
awo akale ngati agwirizana pakati pawo mwaubwino. Ili
ndi lonjezo kwa aliyense amene ali pakati panu amene
amakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza.
Zimenezo ndi zabwino ndi zoyenera kwa inu. Mulungu
ndiye amene amadziwa zonse koma inu simudziwa.
233. Amayi adzayamwitsa ana awo zaka ziwiri zathunthu,
izi ndi za makolo amene afuna kukwaniritsa kuyamwitsa.
Koma ndi udindo wa atate kupereka chakudya ndi zovala za
amai potsatira malamulo. Munthu sadzanyamula chinthu
chimene sangathe kuchichita. Mayi asazunzidwe chifukwa
cha mwana wake kapena bambo asavutitsidwe chifukwa
cha mwana wake. Udindo umenewu umagweranso aliyense
amene alowa chokolo. Koma ngati onse agwirizana kuti
amuletse kuyamwa mwana, iwo sadzakhala ndi mlandu.
Ngati inu muganiza kuti wina akuyamwitsireni mwana
wanu, sikulakwa ngati inu mumulipira mtengo umene
mwagwirizana. Ndipo opani Mulungu, ndipo dziwani kuti
Mulungu amaona zimene muchita.
234. Ndipo iwo amene akufa ndi kusiya akazi, akaziwo
ayenera kudikira, osakwatiwa miyezi inayi ndi masiku
khumi, ndipo iwo akakwaniritsa nthawi iyi, inu
simudzakhala ndi mlandu pa zimene iwo achita molingana
ndi malamulo. Ndipo Mulungu amadziwa zonse zimene
mumachita.
235. Siudzakhala mlandu kwa inu ngati
muonetsa chidwi choti mudzawafunsira chikwati amayi

ofedwa kapena kuwaganizira m'mitima mwanu. Mulungu amadziwa kuti inu mudzawakumbukira iwo. Koma inu musapereke lonjezo la ukwati mwa mseri, koma lankhulani nawo mwaulemu. Ndipo inu musawakwatire nthawi yawo yodikira isanathe. Ndipo dziwani kuti Mulungu amadziwa zimene zili m'mitima mwanu, kotero muopeni Iye ndipo dziwani kuti Mulungu ndi wokhululukira ndi wopilira. 236. Simlandu kwa inu ngati musudzula akazi musanalowane nawo kapena musanapereke mphotho ya ukwati. Koma apatseni moyenera, ndipo munthu wolemera apereke molingana ndi chuma chake ndi osauka molingana ndi zimene ali nazo. Mphatso yoyenera ndi udindo kwa ochita zabwino. 237. Ndipo ngati inu muwasudzula musanalowane nawo kupatula pamene mupereka mphatso ya ukwati, agawireni theka la mphatso ya ukwati kupatula ngati iwo akana kulandira kapena mwamuna avomeleza kuti akhoza kumusiyira theka la mphatsoyo. Ndipo ngati mwamuna asiya mphatsoyo ndiye kuti iye waonetsa chilungamo. Ndipo musaiwale kuonetsana chifundo pakati panu. Ndithudi Mulungu amaona zochita zanu.

238. Pemphera mapemphero onse panthawi yake makamaka pemphero la pakati. Ndipo imani modzichipetsa pamaso pa Mulungu. 239. Ndipo ngati inu muchita mantha, pempherani chiimirire kapena mutakwera. Ndipo mukakhala pa mtendere, kumbukirani Mulungu monga momwe adakuphunzitsirani zimene simudali kuzidziwa kale. 240. Ndipo iwo amene amwalira ndi kusiya akazi awo, ayenera kusiya malangizo kuti akazi awo ayang'aniridwe chaka chathunthu ndipo kuti asachotsedwe m'nyumba. Koma ngati achoka mwa chifuniro chawo palibe mlandu

kwa inu pa zimene iwo angachite ngati ndi zinthu zabwino. Mulungu ndi wa Mphamvu ndiponso Wanzeru. 241. Amayi osudzulidwa nawonso ayenera kupatsidwa gawo loyenera. Uwu ndi udindo wa anthu onse olungama. 242. Motero Mulungu akukufotokozerani zizindikiro zake kwa inu kuti mukhale wozindikira.

243. Kodi siudawaone iwo amene adachoka zikwi zikwi m'nyumba zawo chifukwa choopa imfa? Ndipo Mulungu adati kwa iwo: "Ifani." Ndipo atatero Iye adawaukitsanso kwa akufa. Ndithudi Mulungu ndi wabwino kwa anthu koma ambiri sayamika. 244. Ndipo menyani nkhondo mu njira ya Mulungu ndipo dziwani kuti Mulungu ndiwakumva ndi wodziwa. 245. Kodi ndani amene angakongoze Mulungu ngongole yabwino kuti Iye adzamuonjezere zambirimbiri? Ndi Mulungu amene amachepetsa ndiponso amachulukitsa ndipo kwa Iye nonsenu mudzabwerera.

246. Kodi iwe siudawone zimene gulu la ana a Israyeli adachita Mose atafa? Pamene iwo adati kwa Mtumwi wawo: "Tisankhire Mfumu," ndipo ife tidzamenya nkhondo m'njira ya Mulungu. Iye adati: "Kodi inu simungamenye nkhondo ngati mutalamulidwa kutero?" Iwo adati: "Kodi ife tingakane bwanji kumenya nkhondo mmene afunira Mulungu pamene ife tidaumilizidwa kuchoka m'nyumba mwathu ndi kusiya ana athu?" Koma pamene adalamulidwa kuti amenye nkhondo, onse adathawa kupatula anthu owerengeka okha. Ndipo Mulungu amadziwa anthu osalungama. 247. Ndipo Mtumwi wawo adati kwa iwo: Ndithudi Mulungu wasankha Saulo kuti akhale Mfumu yanu. Iwo adati: "Iye angapatsidwe bwanji Ufumu pamene ife ndife oyenera kukhala Mfumu m'malo mwa iye ndipo

iye alibe chuma chambiri?" Iye adati: "Ndithudi Mulungu wamusankha iye m'malo mwa inuyo ndipo Mulungu wamuonjezera nzeru zambiri ndiponso mphamvu. Ndipo Mulungu amapereka Ufumu kwa aliyense amene Iye wamufuna. Ndipo Mulungu sasowa chilichonse ndiponso amadziwa chinthu china chilichonse." 248. Ndipo Mtumwi wawo adati kwa iwo: Ndithudi! Chizindikiro cha ufumu wake ndi chakuti kudzadza kwa inu Likasa la malamulo limene lidzakhala ndi mtendere wochokera kwa Ambuye wanu ndi nyenyeswa zimene adasiya anthu a banja la Mose ndi a banja la Aroni litanyamulidwa ndi angelo. Ndithudi mu ichi muli chizindikiro kwa inu muli okhulupirira."

249. Ndipo pamene Saulo ananyamuka ndi gulu lake la nkhondo, iye adati: "Ndithudi! Mulungu adzakuyesani pa mtsinje. Motero aliyense amene adzamwa madzi pamenepo sadzakhala wa gulu langa, ndipo yense amene sadzamwa adzakhala wa gulu langa, kupatula yekhayo amene adzatunge muyeso wa pa chikhato pake." Koma padali kagulu kochepa kamene kadamwa motero. Motero iye atawoloka mtsinjewo, iye ndi iwo amene adakukhulupirira mwa iye, adati: "Ife lero tilibe mphamvu zogonjetsera Goliati ndi Asirikali ake." Koma iwo amene adali ndi chikukhulupiririro choti adzakumana ndi Ambuye wawo adati: "Kodi ndi kangati kagulu kochepa kamagonjetsa chigulu cha nkhondo ndi chilolezo cha Mulungu? Ndipo Mulungu amakhala pamodzi ndi opirira." 250. Ndipo pamene iwo anadza kudzakumana ndi Goliati ndi Asirikali ake, iwo adati: "Ambuye wathu! Dzadzani mitima yathu ndi chipiriro ndipo tithandizeni kugonjetsa anthu osakhulupirira." 251. Mwa chifuniro cha Mulungu, iwo anamenya nkhondo.

Davide anapha Goliati ndipo Mulungu anamupatsa iye
ufumu ndi luntha ndipo anamuphunzitsa zimene Mulungu
adafuna. Akanakhala kuti Mulungu satchinjiriza anthu ena
ndi anzawo, dziko lonse likanaonongeka. Koma Mulungu
ndi wopereka moolowa manja kwa zolengedwa zonse.
252. Amenewa ndi Mau a Mulungu tili kulakatula kwa iwe ndi
choonadi chonse. Ndithudi iwe ndiwe mmodzi wa Atumwi
athu. 253. Atumwi aja! Ife tidawakweza ena kuposa anzawo.
Kwa ena a iwo Mulungu adalankhula nawo mwachindunji,
pamene ena adawakweza kukhala a pamwamba ndipo
kwa Yesu mwana wa Mwamuna wa Maria, Ife tidampatsa
zizindikiro zooneka ndipo tidamulimbikitsa ndi Mzimu
Woyera. Mulungu akadafuna, iwo amene adadza pambuyo
pawo sakadamenyana wina ndi mnzake pamene zizindikiro
zooneka zitadza kwa iwo, koma iwo adakangana. Ena adali
ndi chikhulupiriro pamene ena mwa iwo adakana. Koma
Mulungu akadafuna, iwo sakadamenyana wina ndi mzake
ayi. Mulungu amachita chimene wafuna.
254. Oh Inu anthu okhulupirira! Perekani gawo la zimene
takupatsani lisanafike tsiku limene sikudzakhala malonda,
ubwenzi kapena mkhalapakati. Ndithudi ndi anthu
osakhulupirira amene ali osalungama. 255. Mulungu! Kulibe
mulungu wina koma Iye yekha, Wamoyo ndi Wamuyaya.
Iye saodzera kapena kugona. Zake ndi zonse zimene zili
kumwamba ndi padziko lapansi. Ndani amene angakhale
mkhalapakati pa Iye opanda chilolezo chake? Iye amadziwa
zonse zimene zimachitika mdziko lino ndi zimene
zidzachitike m'moyo uli nkudza. Ndipo iwo sadzadziwa
chilichonse kuchokera ku nzeru zake pokhapokha ngati Iye
afuna. Mpando wake umafika kumwamba ndi dziko lapansi.

Ndipo chisamaliro chake pazinthu zonse sichimutopetsa
ayi. Iye ndi wapamwamba mwamba ndi Wamkulu zedi.
256. Palibe kukakamizana m'chipembedzo. Ndithudi njira
yoyenera yaonekera kusiyana ndi njira yolakwa. Iye amene
asiya kupembedza mafano ndipo aika chikhulupiriro chake
mwa Mulungu, ndithudi wagwiritsitsa chingwe chimene
sichidzaduka. Ndipo Mulungu ndi wakumva ndi wodziwa.
257. Mulungu ndi Mtetezi wa amene akhulupirira. Iye
amawatulutsa kuchokera ku mdima kupita nawo kowala.
Koma iwo amene sakhulupirira, owathandiza wawo ndi
Satana, amene amatulutsa iwo kuchoka kowala kupita
ku mdima. Iwo ndiwo anthu aku moto ndipo adzakhala
komweko mpaka kalekale.

258. Kodi iwe siudamuone iye amene anatsutsana ndi
Abrahamu pa nkhani ya Ambuye wake chifukwa cha kuti
Mulungu anamupatsa iye ufumu? Pamene Abrahamu adati:
"Ambuye wanga ndiye amene amapereka moyo ndi imfa."
Iye adati: "Ine ndimapereka moyo ndi imfa." Abrahamu
adati: "Ndithudi Mulungu amatulutsa dzuwa kuchokera ku
m'mawa choncho iwe ulitulutse kuchokera ku madzulo."
Munthu wosakhulupirira uja adathedwa nzeru. Mulungu
satsogolera anthu ochita zoipa.

259. Kapena iye amene adadutsa Mumzinda umene
udaonongeka ndi kusanduka bwinja ndipo adanena kuti:
"Kodi Mulungu angapereke moyo bwanji ku Mzinda
pamene utafa?" Motero Mulungu adamupha iye ndipo
patatha zaka zana limodzi Iye adamuukitsa kwa akufa.
Mulungu adati: "Kodi iwe wakhala chifere nthawi yotani?"
Iye adati: "Mwina tsiku limodzi kapena maola owerengeka
basi." Mulungu adati: "Iyayi, iwe wakhala zaka zana limodzi.

Taona chakudya chako ndi chakumwa chako, sizinasinthe ayi ndipo taona bulu wako! Ife tikusandutsa kuti ukhale chizindikiro kwa anthu. Ndipo taona mafupa m'mene timawaikira pamodzi ndi kuwakuta ndi mnofu." Ndipo pamene zonse zinaonetsedwa kwa iye, iye adati: "Ndadziwa tsopano kuti Mulungu ali ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse." 260. Ndipo pamene Abrahamu adati: "Ambuye wanga! Ndionetseni mmene Inu mumaukitsira zinthu zakufa." Mulungu adati: "Kodi iwe siukhulupirira?" Abrahamu adati: "Ndimakhulupirira, koma ndifuna kuti ndikhutitsidwe mumtima mwanga." Mulungu adati: "Tenga mbalame zinayi ndipo uziwete kenaka uziphe ndi kuika pa phiri lililonse zigawozigawo za mbalame ndipo uziitane. Ndipo izo zibwera kwa iwe mwaliwiro. Ndipo dziwa kuti Mulungu ndi Wamphamvu ndi Wanzeru."

261. Kufanana kwa amene amapereka chuma chawo m'njira ya Mulungu kuli ngati njere ya tirigu imene imabereka njere zina zisanu ndi ziwiri ndipo ililonse imabereka njere zana limodzi. Mulungu amapereka moolowa manja kwa amene wamufuna. Ndipo Mulungu ali ndi zonse zimene zolengedwa zake zimafuna. Iye amadziwa chinthu china chilichonse. 262. Iwo amene amapereka chuma chawo m'njira ya Mulungu ndipo sakumba wina aliyense chifukwa cha choperekacho kapena mtozo, mphotho yawo ili ndi Ambuye wawo. Iwo sadzaopa kapena kudandaula. 263. Mawu abwino ndi chikhululukiro ndi zinthu zabwino kuposa chopereka chaulere chimene chimatsatiridwa ndi kutafula. Mulungu ndi Wolemera ndipo ndi Wopirira kwambiri. 264. Oh Inu anthu okhulupirira! Musaononge zopereka zanu zaulere pokumbutsa kapena kunyoza. Monga amene

amapereka chuma chake ndi cholinga chodzionetsera kwa anthu ndipo sakhulupirira mwa Mulungu kapena mwa tsiku la chimaliziro iye ali ngati mwala umene wakutidwa ndi nthaka ndipo pamene mawawa a mvula agwa iwo umaonekera pa mtunda. Iwo sangathe kuchita chilichonse ndi zimene amapeza. Mulungu satsogolera anthu osakhulupirira.

265. Ndipo iwo amene amapereka chuma chawo ndi cholinga chokondweretsa Mulungu ndi kulimbikitsa chikhulupiriro m'mitima mwawo, ali ngati munda umene uli pamalo pokwera, ndipo pamene mvula igwa pa iwo, umabereka zakudya mowirikiza. Ndipo ngati mvula siigwa, iwo umathiriridwa ndi mame. Ndipo Mulungu amaona zonse zimene mumachita. 266. Kodi wina wa inu angakonde kukhala ndi munda wa tende ndi azitona womwe umathiriridwa ndi mitsinje pansi pake ndipo uli ndi zipatso zosiyanasiyana, pamene ukalamba wampeza, pomwe iye ali ndi ana opanda mphamvu ndipo munda uja uli kukunthidwa ndi mphepo ndipo m'kati mwa mphepoyo muli moto umene utentha mundawo? Kotero Mulungu ali kufotokoza chivumbuluitso chake momveka kwa inu kuti muganize bwino.

267. Oh inu anthu okhulupirira! Perekani chopereka cha ulere kuchokera ku chuma chimene mwachipeza mwa chilungamo ndiponso icho chimene Ife takupatsani kuchokera ku nthaka ndipo musamasankha kupereka chinthu chimene inu simungathe kulandira pokhapokha mutatseka maso anu. Ndipo dziwani kuti Mulungu ndi wolemera ndiponso woyenera kulemekezedwa. 268. Satana ali kukuopsezani ndi umphawi ndipo ali kukulamulirani

kuchita zoipa pamene Mulungu ali kukulonjezani chikhulululukiro ndi zabwino. Ndipo Mulungu ali ndi zonse zimene zolengedwa zake zimafuna. Iye amadziwa chinthu china chilichonse. [269.] Iye amapereka luntha kwa iye amene wamufuna ndipo iye amene wapatsidwa luntha, ndithudi, wapatsidwa chinthu chabwino kwambiri. Koma palibe wina aliyense amene amakumbukira kupatula anthu ozindikira.

[270.] Chopereka chilichonse chimene mupereka kapena malonjezo ena alionse amene mulonjeza, khulupiririrani kuti Mulungu amazidziwa. Ndipo anthu ochita zoipa alibe wina aliyense owathandiza. [271.] Kuulula chimene mwapereka ndi bwino koma kupereka mwa mseri kwa anthu osauka ndi kwabwino kwambiri. Mulungu adzakukhululukirani ena mwa machimo anu. Ndipo Mulungu amadziwa chinthu china chilichonse chimene mumachita. [272.] Si udindo wako kuwatsogolera iwo koma Mulungu ndiye amene amatsogolera amene Iye wamufuna. Ndipo chopereka chaulere chilichonse chimene mupereka ndi chabwino kwa inu ndipo musapereke pokhapokha ngati mufuna chisangalalo cha Mulungu. Ndipo chopereka chonse chimene mupereka, chidzabwezedwa kwa inu champhumphu ndipo inu simudzaponderezedwa ngakhale ndi pang'ono pomwe. [273.] Chopereka chaulere chiperekedwe kwa osauka amene atangwanika ndi ntchito ya Mulungu ndipo sangathe kuyenda padziko. Munthu amene sawadziwa amaganiza kuti, chifukwa chodzichepetsa kwawo, iwo sasowa chilichonse. Iwe udzawadziwa chifukwa cha maonekedwe awo. Iwo sapempha ayi. Ndipo chilichonse chabwino chimene upereka, ndithudi Mulungu

amachidziwa bwino kwambiri. 274. Onse amene amapereka chaulere masana kapena usiku, mseri ndi moonekera, adzalandira malipiro awo kuchokera kwa Ambuye wawo. Iwo alibe choti aope ndipo sadzakhumudwa.

275. Iwo amene amadya ndalama za katapira, adzaima maimidwe a munthu amene wamenyedwa ndi Satana ndi kumuyambitsa misala. Ichi ndi chifukwa chakuti iwo amanena kuti: “Katapira ali chimodzimodzi ndi kugulitsa malonda.” Pamene Mulungu adaloleza malonda, Iye adakaniza katapira. Ndipo iye amene alandira chidzudzulo kuchokera kwa Ambuye wake, ndipo aleka, adzakhululukidwa zochimwa zake zakale koma nkhani yake ili m’manja mwa Mulungu. Koma iye amene abwerezanso kudya ndalama za katapira iye adzaponyedwa ku moto wa ku Gahena ndipo iwo adzakhala komweko mpaka kalekale. 276. Mulungu sadalitsa ndalama za katapira koma amadalitsa chopereka chaulere. Iye alibe chikondi pa anthu osakhulupirira ndiponso ochimwa. 277. Ndithudi onse amene ali ndi chikhulupiriro ndipo amachita ntchito zabwino, amasamala mapemphero awo ndi kupereka chopereka chothandizira anthu osauka, adzalipidwa ndi Ambuye wawo. Ndipo iwo sadzaopa china chilichonse kapena kudandaula.

278. Oh inu anthu okhulupirira! Muopeni Mulungu ndipo musalandire gawo lina lililonse loti lidze kwa inu kuchokera ku katapira ngati chikhulupiriro chanu ndi choonadi. 279. Ndipo ngati simusiya izi, yembekezani nkhondo kuchokera kwa Mulungu pamodzi ndi Mtumwi wake. Koma ngati inu mulapa, inu mudzalandira zinthu zanu zoyamba. Musapondereze anzanu ndipo nanunso

simudzaponderezedwa ayi. 280. Ngati munthu amene
ali nanu ndi ngongole ali pa mavuto a chuma, mupatseni
nthawi mpaka pamene angakubwezereni koma ngati
inu musandutsa ngongoleyi kukhala ngati chopereka
chanu chaulere, zotere zidzakhala zabwino kwa inu,
ngati mukadadziwa. 281. Ndipo liopeni tsiku limene
mudzabwerera kwa Mulungu. Ndipo mzimu uliwonse
udzalipidwa molingana ndi ntchito zake, ndipo palibe
amene adzaponderezedwa.
282. Oh inu anthu okhulupirira! Pamene mukongola
ngongole yoperekedwa panthawi yomwe mwagwirizana,
lembani pena pake. Mlembi alembe zonse mwachilungamo.
Ndipo iye asakane kulemba monga mmene Mulungu
wamuphunzitsira, motero alembe. Ndipo mulekeni
wokongola kuti anene zoti zilembedwe ndipo ayenera kuopa
Mulungu Ambuye wake ndipo iye asabise mangawa ena
aliwonse amene ali nawo. Koma ngati munthu wokongolayo
ndi wozerezeka kapena wofoka kapena amene sangathe
kuyankhula, muloleni m’bale wake kuti ayankhule m’malo
mwa iye komatu mwachilungamo. Ndipo itanani amuna
awiri amene ali pakati panu kuti akhale mboni. Ndipo
ngati anthu amuna sangathe kupezeka, funani mwamuna
mmodzi ndi akazi awiri amene mungavomereze kukhala
mboni, kuti achitire umboni; kuti ngati wina wa iwo alakwa,
wina adzakumbutse mnzake. Ndipo mboni zisamakane
kupereka umboni ngati ziitanidwa kutero. Kotero
musatope kulemba ngongole zanu kaya ndi yaing’ono
kapena yaikulu, ndipo mulembenso tsiku lodzabwezedwa
ngongoleyi. Ichi ndicho chilungamo pamaso pa Mulungu,
ndipo zimakhala dongosolo pofuna kutsimikiza ndiponso

ndi njira yabwino kuti musakaike kupatula ngati zimene zili kugulitsidwa ndi zinthu zopezeka mwa mwayi ndipo ndi zoti zigulitsidwe msangamsanga, si mlandu ngati inu simulemba. Koma onetsetsani kuti pali mboni pamene muli kugulitsana wina ndi mnzake. Ndipo pasakhale vuto kwa mlembi kapena wochitira umboni koma ngati mutero mudzalakwa. Motero opani Mulungu chifukwa amakuphunzitsani inu. Ndipo Mulungu amadziwa chinthu china chilichonse. 283. Koma ngati inu muli pa ulendo ndipo simunapeze mlembi, perekani chinthu choti wina agwirizire ngati chikole ndipo ngati wina wa inu asungitsa katundu kwa mnzake, wosunga uja amubwezere mnzakeyo katundu wake ndipo iye aope Mulungu, Ambuye wake. Inu musabise umboni chifukwa aliyense amene abisa umboni ndi ochimwa. Ndipo Mulungu amadziwa zimene mumachita.

284. Mwini wa zonse zimene zili kumwamba ndi pa dziko lapansi ndi Mulungu. Kaya inu muulula za m'maganizo anu kapena mubisa, Mulungu adzakufunsani za izo. Iye amakhululukira aliyense amene Iye wamufuna ndipo amalanga aliyense amene Iye wamufuna . Mulungu ali ndi mphamvu pa chinthu china chili chonse. 285. Mtumwi amakhulupirira mu zimene zavumbulutsidwa kwa iye kuchokera kwa Ambuye wake, ndipo nawonso anthu okhulupirira amatero. Aliyense amakhulupirira mwa Mulungu, Angelo ake, mabuku ake ndi mwa Atumwi ake. Iwo amati "Ife sitisiyanitsa aliyense pakati pa Atumwi ake;" ndipo adati: "Ife tamva ndipo titsatira. Tipempha chikhululukiliro chanu Ambuye chifukwa ndi kwa inu kumene tidzabwerera." 286. Mulungu sapereka katundu

wolemera pa mzimu umene siungathe kumunyamula. Mzimu uliwonse umalandira chilichonse chabwino chimene umachita kapena umalangidwa chifukwa cha ntchito zake zoipa zimene umachita. Pemphani kuti: "Ambuye wathu! Musatilange ife ngati tiiwala kapena tilakwa. Ambuye wathu! Musatikundikire ife mavuto monga amene mudakundikira anthu amene adalipo kale. Ambuye wathu! Musatisenzetse zinthu zimene sitingathe kuzinyamula. Tichotsereni machimo, tikhululukireni ndipo tichitireni chifundo ife. Inu nokha ndinu Mtetezi wathu. Tipatseni kupambana pakati pa anthu osakhulupirira."

Sura 3 • Al 'Imrân

# Al Imran

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha.

1. *Alif Lam Mim.*

2. Mulungu! Kulibe Mulungu wina koma Iye yekha.
Wamuyaya ndi Msungi wa zinthu zonse. 3. Ndiye
amene wavumbulutsa kwa iwe Buku la choonadi,
kutsimikiza mawu amene adaperekedwa kale. Ndipo Iye
anavumbulutsa Buku la chipangano chakale ndi Buku la
chipangano chatsopano. 4. Kale ngati ulangizi kwa anthu
ndipo adatumiza muyeso. Ndithudi iwo amene amakana
chivumbulutso cha Mulungu adzalangidwa kwambiri.
Ndipo Mulungu ndi wamphamvu ndiponso Mwini
kubwezera. 5. Ndithudi palibe chinthu chimene chili

padziko lapansi kapena kumwamba chimene chimabisika
kwa Mulungu. [6.] Iye ndiye amene amakukonzani pamene
muli m'mimba mwa amayi anu mwa chifuniro chake.
Kulibe Mulungu wina koma Iye yekha, Mwini mphamvu
ndi Mwini nzeru.
[7.] Ndiye amene wavumbulutsa kwa iwe Buku. Ndipo ena
mwa mavesi ake ali ndi matanthauzo ozindikirika, omwe ndi
maziko a Buku, pamene ena ndi ovuta kuwazindikira. Ndipo
iwo amene mitima yawo yadzazidwa ndi chisokonekero,
iwo amatsatira mavesi amene ndi ovuta kuwazindikira
ndi cholinga chofuna chisokonezo ndi kufuna kupereka
matanthauzo awoawo. Koma palibe amene amadziwa
matanthauzo ake kupatula Mulungu. Ndipo iwo amene
ali ndi nzeru amati: "Ife timakhulupirira mwa ilo chifukwa
lonse ndi lochokera kwa Ambuye wathu." Ndipo palibe
amene amalabadira kupatula okhawo amene ali ndi nzeru.
[8.] Oh Ambuye wathu! Musalole kuti mitima yathu isokere
pamene Inu mwatilangiza ndipo tipatseni chisomo chanu.
Ndithudi Inu ndinu opereka moolowa manja. [9.] Oh
Ambuye wathu! Ndithudi Inu mudzasonkhanitsa anthu
onse kudza kwa Inu pa tsiku lopanda chikaiko. Ndithudi
Mulungu saphwanya lonjezo lake.
[10.] Ndithudi iwo amene sakhulupirira, chuma chawo
ndiponso ana awo sadzatha kuwapulumutsa ku mkwiyo
wa Mulungu ndipo iwo adzakhala nkhuni za ku Gahena.
[11.] Monga anthu a Farawo ndi iwo amene adalipo kale,
iwo adakana chivumbulutso chathu, motero Mulungu
adawalanga chifukwa cha machimo awo. Mulungu
amakhwimitsa chilango chake. [12.] Nena kwa anthu
amene sakhulupirira: "Inu mudzagonjetsedwa ndi

kusonkhanitsidwa kupita ku Gahena omwe ndi malo oipa
kukhalako." 13. Ndithudi mudali chizindikiro kwa inu,
m'magulu awiri ankhondo, amene adakumana pamalo
omenyera nkhondo. Gulu lina linali kumenya nkhondo
munjira ya Mulungu pamene lina linali gulu la anthu
osakhulupirira. Anthu okhulupirira adaona ndi maso
awo kuti anthu osakhulupirira adali ambiri kuposa iwo.
Koma Mulungu amapereka mphamvu ndi chipulumutso
chake kwa amene wamufuna. Ndithudi mu zimenezi muli
phunziro kwa anthu ozindikira.
14. Zokoma kwa amuna ndi chikondi chimene ali nacho
pa zinthu zimene apeza, akazi, ana, chuma cha golide ndi
siliva chimene chasonkhanitsidwa, mahatchi okongola,
ziweto ndipo minda yolimidwa bwino. Ichi ndi chisangalalo
cha m'moyo uno koma Mulungu ali ndi zinthu zabwino.
15. Nena: "Kodi ine ndikuuzeni zinthu zabwino kuposa izi?
Kwa anthu olungama kuli minda imene ili ndi Ambuye
wawo,yoyenda madzi pansi pake, imene adzakhalako
mpaka kalekale ndipo adzapatsidwa akazi abwino chimene
chili chisomo chochokera kwa Ambuye wawo. Mulungu
ali kuwaona akapolo ake." 16. Iwo amene amati: "Ambuye
wathu! Ife timakhulupirira mwa Inu kotero tikhululukireni
machimo athu ndipo titetezeni kuchilango chamoto."
17. Iwo amene ali opirira, a chilungamo, omvera ndi woolowa
manja, ndipo iwo ndi amene amapempha chikhululukiro
kwa Mulungu nthawi ya m'mawa.
18. Mulungu achitira umboni kuti kulibe mulungu wina
koma Iye yekha ndipo angelo ake ndi anthu ozindikira,
nawo amachitira umboni, Iye amasamala zolengedwa zake
mwa chilungamo. Kulibe mulungu wina koma Iye yekha,

Mwini mphamvu zonse ndi Mwini nzeru. 19. Ndithudi chipembedzo cha Mulungu ndi Chisilamu. Iwo amene adapatsidwa Buku sadagawikane pa chifukwa china chili chonse koma nsanje pamene nzeru zidadza kwa iwo. Ndipo aliyense amene akana zizindikiro za Mulungu, ndithudi, Mulungu ndi wachangu polanga. 20. Ndipo ngati iwo atsutsana nawe, nena: “Ine ndadzipereka kwa Mulungu pamodzi ndi anthu onse amene anditsatira ine.” Ndipo nena kwa iwo amene adalandira Buku kale ndi kwa iwo amene ali mbuli kuti: “Kodi inu mwadzipereka?” Ngati iwo adzipereka, iwo ndi otsogozedwa koma ngati salabadira, iwe ntchito yako ndi kupereka uthenga ndipo Mulungu amaona akapolo ake. 21. Ndithudi iwo amene sakhulupirira chivumbulutso cha Mulungu ndipo kumapha Atumwi mosayenera, ndipo amapha anthu amene amalamulira kuchita chilungamo, auzeni za chilango chowawa. 22. Amenewa ndiwo amene ntchito zawo zidzakhala zopanda pake m’dziko lino ndi m’dziko limene lili nkudza ndipo iwo sadzapeza owathandiza.

23. Kodi siunawaone iwo amene adapatsidwa gawo la Mau a Mulungu? Iwo ali kuitanidwa kuti adzamve mawu amene ali m’Buku la Mulungu kuti aweruzane pakati pawo koma gulu lina mwa iwo limabwerera m’mbuyo ndipo limachita mwano. 24. Ichi ndi chifukwa chakuti iwo amanena kuti: “Ife sitidzakhudzidwa ndi moto kupatula masiku owerengeka okha.” Ndipo chimene iwo amapeka chokhudza chipembedzo chawo, chawasokeretsa iwo. 25. Kodi zidzakhala bwanji pamene Ife tidzawasonkhanitsa pamodzi pa tsiku losakaikitsa? Ndipo mzimu uliwonse udzalipidwa chimene udachita. Ndipo iwo sadzaponderezedwa.

26. Nena: "Oh Ambuye! Mwini Ufumu! Inu mumamupatsa
ufumu aliyense amene mwamufuna ndipo mumalanda
ufumu wa aliyense amene mwamufuna. Inu mumalemekeza
aliyense amene mwamufuna ndi kumpeputsa aliyense
amene mwamufuna. M'manja mwanu muli ubwino
wonse. Ndithudi Inu muli ndi mphamvu pa chinthu china
chilichonse." 27. "Inu mumasanduliza usiku kuti ukhale
usana ndi usana kuti ukhale usiku. Inu mumatulutsa cha
moyo kuchokera ku chakufa ndi chakufa kuchokera ku
chamoyo. Inu mumapereka chuma ndi chakudya moolowa
manja kwa aliyense amene Inu mwamufuna."

28. Anthu okhulupirira asapange ubwenzi ndi anthu
osakhulupirira m'malo mwa anthu okhulupirira, ndipo
aliyense amene achita izi sadzathandizidwa ndi Mulungu
mwanjira ili yonse kupatula ngati inu muopa choipa
chochokera kwa iwo. Ndipo Mulungu ali kukuchenjezani
za chilango chake ndipo pomaliza ndi kwa Mulungu
kumene zonse zidzabwerera. 29. Nena: "Kaya mubisa
zimene zili mumitima mwanu kapena muulula, zonse
Mulungu akuzidziwa. Ndipo Iye amadziwa zonse zimene
zili mlengalenga ndi zimene zili padziko lapansi. Ndipo
Mulungu ali ndi mphamvu pa zinthu zonse." 30. Pa tsiku
limene mzimu uliwonse udzaona zabwino zonse zimene
udachita zitabweretsedwa ndiponso zoipa zonse zimene
udachita, iwo udzafunitsitsa kuti pakadakhala mtunda
wautali pakati pa iwo ndi zoipazo. Ndipo Mulungu ali
kukuchenjezani inu zachilango chake ndipo Mulungu ali
ndi chisoni chambiri kwa akapolo ake. 31. Nena: "Ngati inu,
ndithudi, mukonda Mulungu, nditsatireni ine. Mulungu
adzakukondani ndipo adzakukhululukirani machimo anu.

Mulungu ndi wokhululukira ndi wachisoni chosatha."
32. Nena: "Mverani Mulungu ndi Mtumwi. Koma ngati
simumvera Mulungu sakonda anthu osakhulupirira."
33. Ndithudi Mulungu adasankha Adamu, Nowa ndi
banja la Abrahamu ndi banja la Imran kukhala opambana
mitundu yonse ya nthawi yawo. 34. Ana a wina ndi mnzake
ndipo Mulungu ndi wakumva ndi wodziwa. 35. Pamene
mkazi wa Imran adati: "Ambuye wanga! Ine ndilonjeza
kwa Inu chinthu chimene chili m'mimba mwanga kuti
chidzakhale chokutumikirani Inu. Motero landirani ichi
kuchokera kwa ine ngati nsembe yanga. Ndithudi Inu
ndinu wakumva ndi wozindikira." 36. Ndipo pamene iye
anabereka mwana wake, iye adati: "Ambuye wanga! Ine
ndabereka mwana wamkazi." Koma Mulungu anadziwiratu
chimene iye wabereka. "Ndipo mwana wamwamuna
salingana ndi mwana wa mkazi, ndipo ine ndamutcha
dzina la Maria ndipo ndili kumupereka iye pamodzi
ndi mbewu yake kwa Inu kuti muwateteze kwa Satana
wotembereredwa." 37. Motero Ambuye wake adamulandira
iye, ndi manja awiri. Ndipo Iye anamukuza bwino, ndipo
anamupereka m'manja mwa Zakariya kuti amulere.
Nthawi zonse pamene Zakariya adali kulowa ku chipinda
kumene iye anali kukhala, anali kumupeza ndi chakudya.
Iye adati: "Oh Maria! Kodi chakudya ichi chili kuchokera
kuti?" Iye adati: "Chili kuchokera kwa Mulungu. Ndithudi
Mulungu amapereka chakudya mopanda malire, kwa
aliyense amene wamufuna." 38. Nthawi imeneyo Zakariya
adapempha kwa Ambuye wake nati: "Ambuye wanga!
Ndipatseni ine kuchokera kwa Inu mwana wangwiro. Inu
ndithudi mumamva pemphero." 39. Ndipo pamene iye

adapitiriza mapemphero m'chipinda, angelo anamuitana
iye nati: "Mulungu ali kukuuza nkhani yabwino ya Yohane
amene adzatsimikiza Mawu ochokera kwa Mulungu.
Iye adzakhala wolemekezeka ndi wodzisunga kwa akazi,
Mtumwi wochokera pakati pa anthu angwiro." 40. Zakariya
adati: "Ambuye wanga! Kodi ine ndingakhale ndi mwana
wamwamuna bwanji pamene ine ndine wokalamba ndipo
mkazi wanga ndi wouma?" Iye adati: "Mulungu amachita
chimene Iye wafuna." 41. Iye adati: "Ambuye wanga!
Ndionetseni chizindikiro." Iye adati: "Chizindikiro chako
ndi chakuti iwe siudzayankhula ndi anthu pa masiku atatu
kupatula m'zizindikiro zokhazokha. Ndipo umukumbukire
kwambiri Ambuye wako ndi kumulemekeza madzulo
ndi m'mawa." 42. Ndi pamene angelo adati: "Oh Maria!
Ndithudi Mulungu wakusankha ndi kukuyeretsa iwe ndipo
wakusankha kukhala wapamwamba pakati pa akazi ena a
zolengedwa zonse." 43. "Oh Maria! Khala omvera Ambuye
wako, gwetsa nkhope yako pansi, ndipo werama pamodzi
ndi iwo amene amapembedza mowerama." 44. Iyi ndi
nkhani yobisika imene Ife tili kukuululira. Iwe kudalibe
pamene iwo adachita mayere ndi zolembera zawo oti aone
kuti kodi ndani wa iwo amene ayenera kusamala Maria
ndiponso iwe kudalibe pamene iwo adali kukangana.

45. Ndi pamene angelo adati: "Oh Maria! Ndithudi
Mulungu ali kukupatsa nkhani yabwino ya Mawu ochokera
kwa Iye amene dzina lake ndi Messiya, Yesu mwana wa
Maria, wolemekezeka m'dziko lino ndi m'dziko limene lili
nkudza ndipo adzakhala m'gulu la anthu okhala pafupi ndi
Mulungu." 46. "Iye adzayankhula kwa anthu ali m'chikuta
ndi atakula msinkhu ndipo adzakhala mugulu la anthu

angwiro.” 47. Iye adati: “Oh Ambuye wanga! Kodi ine
ndingabereke mwana bwanji pamene sindidakhudzidwe
ndi mwamuna?” Iye adati: “Zidzakhala choncho, chifukwa
Mulungu amalenga chimene afuna. Ndipo pamene
afuna chinthu, Iye amangonena kwa icho, ‘Khala’ ndipo
chimakhala.” 48. Ndipo Iye adzamuphunzitsa kulemba ndi
luntha, Torah ndi Utenga wabwino. 49. Ndipo adzamupanga
iye kukhala Mtumwi wa ana a Israyeli nati: “Ine ndadza kwa
inu ndi chizindikiro chochokera kwa Ambuye wanu ndipo
kuchokera ku dothi ndidzakuumbirani chinthu chofanana
ndi mbalame ndipo ine ndidzaipumira mpweya ndipo ndi
chilolezo cha Mulungu idzakhala mbalame ya moyo. Ndi
chilolezo cha Mulungu, ine ndidzachiza anthu a khungu,
akhate ndi kuukitsa anthu akufa. Ine ndidzakuuzani
zimene muzidya ndi zimene musunga m’nyumba mwanu.
Ndithudi mu zimenezi muli zizindikiro kwa inu ngati
muli okhulupirira.” 50. “Ndipo ine ndadzatsimikiza zimene
zidalipo pambuyo panga ndi kukulolezani inu kuchita
zina mwa zinthu zimene mudaletsedwa ndipo ine ndadza
ndi chizindikiro chochokera kwa Ambuye wanu. Motero
opani Mulungu ndipo mundimvere ine.” 51. “Ndithudi!
Mulungu ndi Ambuye wanga ndi Ambuye wanu; ‘Motero
m’pembedzeni Iye yekha.’ Imeneyi ndiyo njira yoyenera.”

52. Ndipo pamene Yesu adaona kuti iwo adalibe
chikhulupiriro, iye adati: “Kodi ndani adzandithandiza ine
mu ntchito ya Mulungu?” Ophunzira ake adati: Ife ndife
othandiza mu ntchito ya Mulungu, Ife takhulupirira mwa
Mulungu ndipo chitirani umboni kuti ife ndife Asilamu.
53. “Ambuye wathu! Ife takhulupirira zimene mwavumbulutsa
ndipo titsatira Mtumwi wanu motero tiikeni ife m’gulu

la mboni zanu." 54. Ndipo iwo adachita chiwembu koma
Mulungu adakonza chiwembu chake. Ndipo Mulungu ndi
wodziwa kwambiri pokonza chiwembu. 55. Ndi Pamene
Mulungu adati: "Oh iwe Yesu! Ine ndidzakutenga kudza
kwa Ine ndipo ndidzakuyeretsa kwa anthu osakhulupirira
ndipo ndidzawapanga onse amene amakutsatira iwe
kukhala apamwamba pa iwo amene sakhulupirira mpaka
pa tsiku la kuuka kwa akufa. Ndipo inu mudzabwerera kwa
Ine ndipo Ine ndidzaweruza pa zimene mudali kutsutsana.
56. Akakhala iwo amene sakhulupirira, Ine ndidzawalanga
ndi chilango chowawa m'dziko lino ndi m'dziko limene
lili nkudza ndipo sadzapeza wina wowathandiza.
57. Akakhala iwo amene ndi okhulupirira ndipo amachita
ntchito zabwino, Mulungu adzawalipira mphotho yawo
yokwanira. Ndipo Mulungu sakonda anthu ochita zoipa.
58. Ichi chimene tiri kulakatula kwa iwe ndi Mavesi ndi
Chikumbutso cha nzeru."

59. Ndithudi kulingana kwa Yesu pamaso pa Mulungu ndi
chimodzimodzi ndi Adamu. Iye anamulenga kuchokera
ku dothi ndipo adati kwa iye: "Khala" ndipo adakhala.
60. Ichi ndi choonadi chochokera kwa Ambuye wako,
motero usakhale mmodzi wa anthu okaika. 61. Ndipo iye
amene atsutsana nawe pankhani za Yesu utalandira nzeru
izi muuze kuti: "Bwerani kuti taitane ana athu ndi ana
anu, akazi athu ndi akazi anu, ife ndi inu ndipo tipemphe
modzichepetsa kuti matemberero a Mulungu akhale pa
anthu amene ali nkunama." 62. Ndithudi iyi ndi nkhani
yoona, ndipo kulibe Mulungu wina koma mmodzi yekha.
Ndipo ndithudi, Mulungu ndi Wamphamvu ndi Wanzeru.

63. Ngati iwo sakumvera, ndithudi, Mulungu anadziwa
anthu ochita zoipa.
64. Nena: “Oh inu anthu a m’Buku! Bwerani ku Mau amene
ndi oona pakati pa inu ndi ife, kuti tisapembedze wina
aliyense koma Mulungu mmodzi ndipo tisamuphatikize
ndi china chili chonse ndipo pasakhale wina pakati pathu
amene adzasankha ena ngati ambuye powonjezera pa
Mulungu. Ndipo ngati iwo akana, nena: “Inu chitirani
umboni kuti Ife ndife Asilamu.” 65. “Oh inu anthu a m’Buku!
Kodi ndi chifukwa chiyani mukutsutsana za Abrahamu,
pamene Buku la Chipangano chakale ndi Chipangano
Chatsopano linali lisanavumbulutsidwe panthawi yake?
Kodi mulibe nzeru? 66. Kodi inu ndinu amene mumatsutsana
pa nkhani zimene mumazidziwa? Nanga ndi chifukwa
chiyani mukutsutsana pa zinthu zimene simudziwa?
Ndi Mulungu amene amadziwa ndipo inu simuzidziwa.
67. Abrahamu sadali Myuda kapena Mkhirisitu. Iye adali
munthu wangwiro amene adadzipereka kwathunthu kwa
Mulungu. Iye sadali opembedza mafano ayi. 68. Ndithudi
pakati pa anthu amene ali kufupi ndi Abrahamu, pali
iwo amene adamutsatira iye ndi Mtumwi uyu ndi iwo
amene akhulupirira. Ndipo Mulungu amasamalira anthu
okhulupirira. 69. Ena mwa anthu amene amakhulupirira
Buku amafuna kukusocheretsa iwe. Komatu iwo
sangasocheretse wina aliyense koma iwo eni, ndipo iwo
sazindikira. 70. Oh inu anthu a m’Buku! Bwanji mumakana
zizindikiro za Mulungu pamene inu mumachita umboni?
71. Oh inu anthu a m’Buku! Bwanji mumasakaniza choonadi
ndi bodza ndipo mumabisa choonadi pamene inu muli
kudziwa?

72. Ndipo ena mwa anthu a m'Buku amati: Khulupiririrani
mu zimene zavumbulutsidwa kwa anthu okhulupirira
m'mawa ndipo muzikane madzulo ake kuti iwo akhoza
kubwerera m'mbuyo. 73. Ndipo musakhulupilire wina
aliyense kupatula amene atsatira chipembedzo chanu.
Nena: "Ndithudi! Chilangizo choonadi ndi chilangizo
cha Mulungu" ndipo musakhulupirire kuti wina wake
adzapatsidwa chinthu cholingana ndi chimene chapatsidwa
kwa inu. Kapena iye adzatsutsana nanu pamaso pa Ambuye
wanu. Nena: "Ndithudi zonse zili m'manja mwa Mulungu.
Iye amazipereka kwa aliyense amene Iye wamufuna. Ndipo
Mulungu ali ndi chili chonse chimene zolengedwa zake
zimafuna, Mwini kudziwa chilichonse." 74. Iye amaonetsa
chifundo chake kwa aliyense amene Iye wamufuna ndipo
Mulungu ndiye mwini zinthu zochuluka. 75. Pakati pa anthu
a m'Buku, alipo wina amene ngati ungamusungitse mulu wa
chuma iye adzakubwezera chonse osachotsapo koma pakati
pawo alipo wina amene ngati iwe umusungitsa ndalama
imodzi ya siliva, sadzakubwezera pokhapokha utalimbikira
kuitanitsa. Chifukwa iwo amati: "Ife tilibe njira yonenedwa
pachifukwa cha anthu opanda nzeru." Kotero amanena
zinthu zabodza zokhudza Mulungu pamene iwo akudziwa.
76. Inde, aliyense amene amakwaniritsa lonjezo lake ndi
kuopa Mulungu kwambiri, ndithudi Mulungu amakonda
iwo amene amamuopa Iye.

77. Ndithudi, onse amene amagula phindu lochepa pa
mtengo wa lonjezo la Mulungu, ndi malonjezo awo, iwo
sadzakhala ndi gawo m'moyo umene uli nkudza. Mulungu
sadzalankhula nawo kapena kuwayang'ana patsiku louka
kwa akufa. Iye sadzawayeretsa ndipo iwo adzalandira

chilango chowawa. 78. Ndipo, ndithudi, pakati pawo
pali iwo amene amatembenuza tanthauzo la Buku ndi
malirime awo pamene akuwerenga ndi cholinga chakuti
iwe uziganiza kuti zonse zimene ali kunena ndi zochokera
m'Buku pamene sichoncho ayi, ndipo iwo amati: "Mawu
awa ndi ochokera kwa Mulungu" pamene sadachokere kwa
Mulungu ndipo iwo amanena zabodza zokhudza Mulungu
pamene iwo akudziwa kuti limenelo ndi bodza. 79. Sizili
kwa munthu amene Mulungu adamupatsa Buku lake, nzeru
ndi kuzindikira malamulo a chipembedzo kuti anene kwa
anthu kuti: "Ndipembedzeni ine m'malo mwa Mulungu."
Koma iye akhoza kunena kuti: "Khalani anthu ophunzira
chipembedzo amene amachita zimene adziwa ndi kuuza
anzawo chifukwa inu muli kuphunzitsa Buku ndipo inu
muli kuliphunzira ilo." 80. Ndipo iye sangakulamuleni
kuti musandutse Angelo ndi Atumwi ngati milungu yanu
ayi. Kodi iye akhoza kukulamulirani inu kuti mukhale
anthu osakhulupirira pamene inu mwadzipereka kale kwa
Mulungu?
81. Ndi pamene Mulungu analandira chipangano cha
Atumwi ponena: "Tsatirani chimene ndidakupatsani
kuchokera m'Buku ndi luntha." Ndipo Mtumwi adadza
kudzatsimikiza zimene muli nazo. Inu muyenera
kumukhulupirira ndi kumuthandiza iye. Ndipo Mulungu
adati: "Kodi mwatsimikiza ndi kuvomera udindo umene
ndakhazikitsa pa inu?" Iwo adati: "Ife tavomera." Iye
adati: "Choncho chitirani umboni ndipo Ine ndiri ndi
inu pochitira umboni." 82. Ndipo iwo amene angabwerere
pambuyo pakumva izi ndi wolakwa. 83. Kodi iwo ali kufuna
chipembedzo chosiyana ndi chipembedzo cha Mulungu

pamene zonse zimene zili kumwamba ndi padziko lapansi
zagonjera kwa Iye monyinyirika kapena mosanyinyirika?
Ndipo ndi kwa Iye kumene onse adzabwerera.
84. Nena: “Ife timakhulupirira mwa Mulungu ndi zimene
zavumbulutsidwa kwa ife ndi zimene zinavumbulutsidwa
kwa Abrahamu ndi Ishimayeli, kwa Isake ndi Yakobo,
ndi kwa ana a Yakobo; ndi zimene anapatsidwa Mose,
Yesu ndi kwa Atumwi kuchokera kwa Ambuye wawo. Ife
sitisiyanitsa pakati pawo ayi ndipo ndi kwa Iye kumene
tadzipereka.” 85. Ndipo aliyense amene afuna chipembedzo
china osati chipembezo cha Chisilamu, sichidzaloledwa
kwa iye ndipo m’dziko limene lili nkudza iye adzakhala
mmodzi wa anthu otayika. 86. Kodi Mulungu adzatsogolera
bwanji anthu amene anakana pambuyo pokhulupilira
pamene iwo anachitira umboni woti Mtumwi ndi woona
ndiponso zizindikiro zooneka zitadza kwa iwo? Ndithudi
Mulungu satsogolera anthu ochita zoipa. 87. Iwo malipiro
awo, ndithudi, ndi matemberero ochokera kwa Mulungu,
angelo ndi anthu onse. 88. Iwo adzakhala m’menemo
mpaka kalekale. Chilango chawo sichidzachepetsedwa
ayi kapena kuchedwetsedwa. 89. Kupatula okhawo amene
pambuyo pake alapa machimo awo ndi kuchita nchito
zabwino. Ndithudi Mulungu ndi wokhululukira ndi
Wachisoni chosatha. 90. Ndithudi iwo amene adakana
atayamba akhulupirira ndipo anapitiliza kusakhulupilira
kwawo, kulapa kwawo sikudzavomerezeka. Ndipo iwo ndi
osochera. 91. Ndithudi iwo amene sanakhulupirire, ndipo
akufa ali osakhulupirira, machimo awo sadzakhululukidwa
ngakhale atapereka golide wodzadza dziko lonse lapansi

ngati chodziombolera. Kwa otero, chilango chowawa chili
kuwadikira ndipo iwo sadzapeza aliyense owathandiza.
92. Inu simudzapeza ubwino mpaka mutapereka
zimene mumazikonda kwambiri ndipo zopereka zonse
zimene mupereka, ndithudi Mulungu amazidziwa
bwino. 93. Chakudya chonse chidali chololedwa kwa
ana Israyeli kupatula zimene Israyeli adadziletsa yekha
Buku la Chipangano chakale lisanavumbulutsidwe.
Nena: "Bweretsani Buku la Chipangano chakale ndipo
liwerengeni ngati zimene munena ndi zoona." 94. Ndipo
zitachitika izi, aliyense amene ampekera bodza Mulungu,
otere ndi osakhulupilira. 95. Nena: "Mulungu wanena
choonadi motero tsatirani chipembedzo cha Abrahamu
wangwiro ndipo iye sadali mmodzi wa anthu opembeza
mafano." 96. Ndithudi Nyumba yoyamba kuti anthu
azipembedzeramo ndi ija imene idali ku Mecca, yodzadza
ndi madalitso, ndi malangizo kwa anthu a mitundu yonse.
97. M'menemo muli zizindikiro zooneka, malo a Abrahamu
ndipo aliyense amene alowamo ndi otetezedwa. Kupita
ku Hajji ndi udindo umene anthu ayenera kukwaniritsa
kwa Mulungu makamaka iwo amene ali ndi chuma. Ndipo
aliyense amene sakhulupirira, Mulungu safuna chithandizo
cha zolengedwa zake. 98. Nena: "Inu anthu a m'Buku! Kodi
bwanji mumakana chivumbulutso cha Mulungu pamene
Mulungu amaona yekha zochita zanu zonse?" 99. Nena: "Inu
anthu a m'Buku. Kodi bwanji mumatsekereza anthu amene
akhulupirira kutsatira njira ya Mulungu ndipo mumafuna
kusokoneza pamene inu mudziwa kuti ndi yoyenera?
Ndipo Mulungu amadziwa zonse zimene mumachita."
100. Oh Inu anthu okhulupirira! Ngati inu mumvera

anthu amene anapatsidwa Buku kale iwo adzakubwezerani
kukhala osakhulupirira pamene munali okhulupirira.
101. Kodi simungakhulupirire bwanji pamene mau a
Mulungu ali kulakatulidwa kwa inu ndipo Mtumwi
wake ali pakati panu? Ndipo aliyense amene akakamira
Mulungu, ndithudi iye watsogozedwa m'njira yoyenera.
102. Oh inu anthu okhulupirira! Muopeni Mulungu monga
momwe ayenera kuopedwera. Musafe pokha pokha muli
Asilamu. 103. Ndipo gwiritsani nonsenu, chingwe cha
Mulungu ndipo musagawikane. Kumbukirani zokoma
zimene Mulungu wakuchitirani chifukwa mudali mdani
wa wina ndi mnzake ndipo Iye adayanjanitsa mitima
yanu, ndipo chifukwa cha chisomo chake, muli achibale;
ndipo inu mudali m'mphepete mwadzenje la moto koma
Iye adakupulumutsani ku motowo. Motero Mulungu
ali kufotokoza momveka zizindikiro zake kwa inu, kuti
mukhale otsogozedwa.

104. Pakati panu payenera kukhala gulu la anthu limene
liziitanira ndi kumalamulira zabwino ndi kuletsa zinthu
zoipa. Ndipo ndi iwo amene ali opambana. 105. Ndipo
musakhale ngati iwo amene anagawanikana ndi kusemphana
maganizo pambuyo pakuti zizindikiro zooneka zidabwera
kwa iwo. Ndi chifukwa cha iwo kuli chilango chowawa.
106. Patsiku limene nkhope zina zidzakhala zowala ndi za
chimwemwe pamene zina zidzakhala za kuda. Anthu amene
adzakhala ndi nkhope zakuda adzafunsidwa kuti: "Kodi
inu mudakana chikhulupiriro mutachivomera poyamba?
Motero lawani chilango, chifukwa chokana kukhulupilira."
107. Iwo amene nkhope zawo zidzakhala zowala, adzakhala,
mpaka kalekale, m'chisomo cha Mulungu. 108. Awa ndi Mau

a Mulungu. Ife tili kuwalakatula kwa iwe mwachoonadi
ndipo Mulungu safuna kupondereza zolengedwa zake.
109. Zake ndi zinthu zonse zimene zili kumwamba ndi
padziko lapansi. Ndipo kwa Iye zinthu zonse zidzabwerera.
110. Inu ndinu anthu abwino amene adalengedwera
mtundu wa anthu, inu mumalamulira kuchita zabwino
ndi kuletsa zoipa ndipo mumakhulupilira mwa
Mulungu. Ndipo anthu a m'Buku akadakhulupilira,
zikadawakhalira bwino. Pakati pawo pali ena amene ali
ndi chikhulupiliro, koma ambiri a iwo ndi ochita zoipa. 111.
Iwo sangakupwetekeni ayi, kupatula kukuvutitsani kokha
ndipo ngati iwo amenyana nanu iwo adzakuonetsani misana
yawo ndipo sadzathandizidwa. 112. Iwo adzanyozedwa
kulikonse kumene adzapezeke kupatula ngati atetezedwa
ndi Mulungu ndi anthu. Mkwiyo wa Mulungu ukuyenera
pa iwo. Ndipo manyazi adzakhazikitsidwa pa iwo. Ichi ndi
chifukwa chakuti iwo sadakhulupirire chivumbulutso cha
Mulungu ndipo anapha Atumwi popanda chifukwa. Ichi
ndi chifukwa chakuti adaswa malamulo mopyola muyeso.
113. Onse sali chimodzimodzi. Gulu lina la anthu a m'Buku
ndi anthu angwiro,iwo amawerenga Mawu a Mulungu
nthawi ya usiku ndi kumagunditsa nkhope pansi. 114. Iwo
amakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku la chimaliziro,
amalamulira zolungama ndi kuletsa zoipa ndipo amakhala
ndi changu pochita ntchito zabwino,ndipo iwo ali pamodzi
ndi anthu olungama. 115. Ndipo chabwino chilichonse
chimene achita, palibe chimene chidzakanidwa chifukwa
Mulungu amadziwa anthu olungama. 116. Ndithudi iwo
amene amakana kukhulupirira, chuma chawo ndi ana awo
sadzawathandiza ngakhale ndi pang'ono pomwe polimbana

ndi Mulungu. Iwo ndiwo eni ake a ku Gahena ndipo adzakhala komweko mpaka kalekale. 117. Fanizo la zimene amapereka mu umoyo wa m’dziko lino zili ngati mphepo ya chisanu imene imagwa m’minda ya anthu ochita zoipa ndi kuiononga. Mulungu sadawalakwire ayi koma iwo adadzilakwira okha.

118. Oh inu anthu okhulupirira! Musapalane ubwenzi ndi anthu ena kupatula anthu a chipembedzo chanu. Iwo sadzasiya kukuchitirani zoipa chifukwa iwo afuna kukuonongani. Chidani chawo ndi chooneka chifukwa cha zimene amanena koma zimene zimabisala m’mitima mwawo ndi zoopsya. Ndithudi ife taonetsa zizindikiro zathu poyera kwa inu ngati muli ndi nzeru. 119. Iyayi! Ndinu amene muli kuwakonda iwo koma iwo sakukondani inu ayi ngakhale inu mumakhulupirira mu Mabuku onse. Pamene akumana nanu iwo amati: “Nafenso ndife okhulupirira.” Koma akakhala paokha, amaluma nsonga za zala zawo mokwiya. Nena: “Ifani ndi mkwiyo wanu! Ndithu Mulungu amadziwa zimene zili m’mitima mwanu.” 120. Ngati inu mupeza bwino, iwo amadandaula, koma ngati zovuta zikugwerani, iwo amasangalala. Koma ngati inu mupirira ndi kudziteteza kumachimo, ziwembu zawo sizidzakuononganі ayi. Ndithudi Mulungu amadziwa zochita zawo zonse.

121. Ndi pamene iwe udasiya abale ako m’mawa kukayika anthu okhulupirira ku malo omenyera nkhondo. Mulungu ndi wakumva ndi wodziwa. 122. Pamene magulu anu awiri adali ndi mantha koma Mulungu adali Mtetezi wawo. Ndipo mwa Mulungu anthu okhulupirira ayenera kuika chikhulupiliro chawo. 123. Mulungu adakupambanitsani pa

nkhondo ya ku Badr pamene inu mudali ofoka. Choncho
opani Mulungu kwambiri kuti mukhale othokoza.
124. Pamene iwe udanena kwa anthu okhulupirira: "Kodi
simunakhutitsidwe pamene Ambuye anakuthandizani
ndi angelo zikwi zitatu amene adatsitsidwa kuchokera
kumwamba kuti akuthandizeni?" 125. "Inde, ngati inu
mupirira ndi kukhala angwiro ndipo pamene mdani adza
mofulumira kwa inu, Ambuye wanu adzakuthandizani ndi
angelo zikwi zisanu a zizindikiro." 126. Mulungu adakonza
ichi kuti chikhale nkhani yabwino kwa inu kuti mitima yanu
ikhazikike. Kupambana sikuchokera kwa wina aliyense
koma Mulungu, Mwini mphamvu ndi Mwini nzeru zonse.
127. Kuti Iye akhoza kumwaza gulu la anthu osakhulupirira
kapena kuwanyoza kuti akhoza kumwazikana. 128. Iwe ulibe
lamulo lililonse munkhani iyi. Kaya Iye adzawakhululukira
kapena kuwalanga, ndithudi iwo ndi anthu ochita zoipa.
129. Zake za Mulungu ndi zinthu zonse zimene zili
kumwamba ndi padziko lapansi. Iye amakhululukira
aliyense amene wamufuna ndi kulanga aliyense amene
wamufuna. Mulungu ndi Wokhululukira ndi Wachisoni.

130. Oh inu anthu okhulupirira! Musadye ndalama za
katapila musachulukitse ndalama motero, ndipo opani
Mulungu kuti inu mupambane. 131. Ndipo opani Moto wa
ku Gahena, umene wakonzedwera anthu osakhulupirira.
132. Ndipo mverani Mulungu ndi Mtumwi wake kuti
mupeze chifundo chake. 133. Ndipo fulumirani kukapeza
chikhululukiro cha Ambuye wanu ndi Paradiso imene
kutambasuka kwake kuli ngati kumwamba ndi dziko
lapansi, yokonzedwera anthu oopa Mulungu. 134. Amene
amapereka mu mtendere kapena m'mavuto, ndipo amaleza

mtima akakwiya ndipo amakhululukira anthu. Ndithudi
Mulungu amakonda anthu ochita zabwino. 135. Ndi iwo
amene, ngati achita chigololo kapena alakwira mizimu yawo,
amakumbukira Mulungu ndi kupempha chikhululukiro cha
machimo awo, ndipo palibe wina amene angakhululukire
machimo kupatula Mulungu, ndipo sapitiliza kuchita zoipa
pamene iwo ali nkudziwa. 136. Kwa otere, malipiro awo ndi
chikhululukiro chochokera kwa Ambuye wawo ndi minda
yothiriridwa ndi mitsinje yoyenda pansi pake kumene iwo
adzakhalako mpaka kalekale. Dipo la bwino kwa iwo amene
amachita ntchito zabwino. 137. Anthu akale nawo anaona
mavuto otere. Motero inu yendani padziko lapansi ndipo
muone chimene chidawachitikira anthu osakhulupirira.
138. Awa ndi mawu omveka kwa anthu, chilangizo ndi
chenjezo kwa iwo amene amalewa zoipa.

139. Motero musagwe ulesi kapena kudandaula, inu
mudzapambana, ngati ndinu okhulupirira. 140. Ngati inu
muvulala, zindikirani kuti ena nawo adavulala. Ndipo
masiku sakoma onse ndipo Ife timapereka kwa anthu
mwakasintha sintha kuti Mulungu ayese iwo amene
akhulupirira ndipo kuti akhoza kupha ena kuchokera
ku magulu anu. Ndipo Mulungu sakonda iwo amene
amachita zoipa. 141. Ndi kuti Mulungu ayeretse anthu
okhulupirira ndi kuononga anthu osakhulupirira. 142. Kodi
inu mumaganiza kuti mukalowa ku Paradiso Mulungu
asanadziwe anthu amene anamenya nkhondo m'njira ya
Mulungu ndikuwadziwa amene anapirira? 143. Inu, ndithudi,
munali kufuna imfa musadakumane nayo. Ndipo tsopano
mwaiona mmene imakhalira ndi maso anu.

144. Muhammad siwina aliyense koma Mtumwi ndipo,

ndithudi, Atumwi ena adalipo kale iye asanadze. Ngati iye
akufa kapena aphedwa, kodi inu mudzabwerera m'mbuyo?
Yense amene abwerera m'mbuyo sadzachita chilichonse
chopweteka Mulungu ndipo Mulungu adzalipira anthu
oyamika. 145. Ndipo palibe amene amafa kupatula ndi
chilolezo cha Mulungu ndi pa nthawi yokhazikitsidwa
kale. Ndipo iye amene afuna malipiro a m'dziko lino,
Ife tidzamupatsa ndipo iye amene afuna malipiro a
m'moyo umene uli nkudza Ife tidzamupatsa. Ndipo Ife
tidzalipira anthu othokoza. 146. Ndi Atumwi ambiri amene
adamenya nkhondo ndipo pamodzi ndi iye panali anthu
ambiri odziwa chipembedzo. Koma iwo sadataye mtima
chifukwa cha zimene zidagwa pa iwo m'njira ya Mulungu
kapena kufoka ayi kapena kudzinyoza. Ndipo Mulungu
amakonda anthu opirira. 147. Ndipo iwo sadanene china
koma kuti: "Oh Ambuye! Tikhululukireni machimo
athu ndi kuswa malamulo kwathu. Limbikitsani mapazi
athu ndipo tipambanitseni kwa anthu osakhulupirira."
148. Motero Mulungu adawapatsa mphotho ya m'moyo uno
ndi mphotho yolemekezeka ya m'moyo umene uli nkudza.
Mulungu amakonda anthu olungama.

149. Oh inu anthu okhulupirira! Ngati inu mumvera anthu
osakhulupilira iwo adzakupangani kukhala osakhulupirira
ndipo mudzabwerera ngati otaika. 150. Iyayi, Mulungu
ndiye Mtetezi wanu, ndipo Iye ndiye wothandiza
kupambana wina aliyense. 151. Ife tidzaika mantha
m'mitima ya anthu osakhulupirira chifukwa amatumikira
milungu ina yowojezera pa Mulungu imene iwo sadalandire
chilolezo choti azitumikira. Moto udzakhala mudzi
wawo. Ndithu onyansa kwambiri ndi malo amene anthu

ochita zoipa akakhalako. 152. Ndipo Mulungu, ndithudi, adakwaniritsa lonjezo lake kwa inu pamene inu munali kuwapha ndi chilolezo chake mpaka pamene munafooka ndipo mudayamba kukangana ndipo simunamvere Iye atakulangizani chimene mukonda. Pakati panu pali iwo amene amafuna moyo wa m'mdziko lapansi ndi ena amene afuna moyo umene uli nkudza. Ndipo Iye adakonza kuti muthawe kuti Iye akhoza kukuyesani. Koma, ndithudi, Iye adakukhululukirani inu ndipo Mulungu amaonetsa chifundo kwa anthu okhulupirira. 153. Pamene inu mudathawa osaona kumbali kwa wina aliyense ndipo Mtumwi adali m'mbuyo mwanu kukuitanani. Pamenepo Mulungu anakupatsani vuto powonjezera pa vuto lina ngati kubwezera ndi cholinga chokuphunzitsani inu kuti musamve chisoni pa zimene simunazipeze kapena zimene zinadza kwa inu. Mulungu amadziwa zonse zimene mumachita.

154. Ndipo chitantha chisoni, adakutsitsirani mtendere kuti udze pa inu. Ndipo tulo tidagwira ena a inu pamene ena adangogona kumavutika m'maganizo, chifukwa cha zilakolako zawo, kuganiza mosalungama ndikukhala ndi maganizo a umbuli okhudza Mulungu. Iwo adafunsa: "Kodi ife tili ndi chonena pankhani iyi?" Nena: "Zonse zili m'manja mwa Mulungu." Iwo amabisa m'mitima mwawo zinthu zimene safuna kuulula kwa iwe. Iwo amanena kuti: "Tikadakhala kuti tidaloledwa kunenapo maganizo athu pankhaniyi, ife sitikanaphedwa pano." Nena: "Ngakhale inu mukadakhala kunyumba zanu ndithudi ena amene adalembedwa kuti aphedwe akadapita ku malo kumene akadakaphedwa." Ndipo Mulungu adachita zimenezi kuti

ayese zimene zili m'mitima mwanu ndi kuyeretsa zimene
zili m'mitima mwanu ndipo ndithudi Mulungu akudziwa
zimene zili m'mitima. 155. Ena a inu amene mudathawa
patsiku limene anthu a magulu awiri ankhondo adakumana,
ndi Satana amene adawapangitsa kuti athawe zimene
adachita. Zoonadi Mulungu adawakhululukira. Ndithudi
Mulungu ndi okhululukira ndi wopilira kwambiri.
156. Oh inu anthu okhulupirira! Musakhale ngati
osakhulupirira amene amanena kwa abale awo pamene
ayenda padziko kapena apita kunkhondo: "Akadakhala kuti
adali ndi ife kuno, iwo sakadafa ayi kapena sakadaphedwa."
Mulungu amatero kuti iwo adzakumbukire mawu awo. Ndi
Mulungu amene amapereka moyo ndi imfa. Ndipo Mulungu
amaona ntchito zonse zimene mumachita. 157. Ndipo
ngati inu muphedwa kapena mukufa mnjira ya Mulungu,
chikhululukiro ndi chifundo chochokera kwa Mulungu
ndi chabwino kuposa chuma chimene akusonkhanitsa.
158. Ngati inu muphedwa kapena mufa, ndithudi ndi kwa
Mulungu kumene nonse mudzasonkhanitsidwa. 159. Ndi
chifundo cha Mulungu iwe udakhala nawo mwa ufulu.
Ndipo iwe ukadakhala wa nkhanza kapena owuma mtima,
ndithudi onse akadakuthawira. Motero akhululukire
ndipo pempha kuti awakhululukire ndipo kambirana
nawo. Ndipo ukatsimikiza, ika chikhulupiriro chako mwa
Mulungu. Ndithudi Mulungu amakonda iwo amene amaika
chikhulupiliriro chawo mwa Iye. 160. Ngati Mulungu
akuthandizani inu, palibe amene angakugonjetseni ndipo
ngati Iye atakutayani, kodi ndani amene angakuthandizeni
inu kupatula Iye yekha? Ndipo mwa Mulungu onse
okhulupirira ayenera kuika chikhulupiriro chawo.

161. Ndikosaloledwa kuti Mtumwi wina aliyense atenge
katundu wopeza munkhondo mopanda kulamulidwa
ndipo aliyense amene anyenga omutsatira ake pa nkhani ya
chuma chopeza ku nkhondo, adzanyamula patsiku louka
kwa akufa zimene iye anatenga mopanda chilolezo. Ndipo
munthu aliyense adzalipidwa molingana ndi zochita zake
ndipo iwo sadzaponderezedwa ai. 162. Kodi munthu amene
atsata zokondweretsa Mulungu angafanizidwe ndi munthu
amene walandira mkwiyo wa Mulungu? Gahena idzakhala
mudzi wake ndipo malo omwe adzakhalako ndi onyansa.
163. Iwo ali m'magulu osiyana siyana pamaso pa Mulungu.
Ndipo Mulungu ali kuona chili chonse chimene amachita.
164. Ndithudi Mulungu anaika chisomo chake pa anthu
okhulupirira pamene anatumiza pakati pawo Mtumwi
wochokera pakati pawo kudzawawerengera chivumbulutso
chake ndi kuwayeretsa ndi kuwaphunzitsa Buku ndi luntha;
angakhale kuti iwo kale adali anthu osochera moonetsera.

165. Pamene mavuto adza pa inu ngakhale kuti inu
mudapha anthu kwambiri, inu mudati: "Kodi zichokera
kuti izi?" Nena: "Zimenezi zichokera kwa inu nomwe.
Ndithudi Mulungu ali ndi mphamvu pa chinthu china
chilichonse." 166. Kugonjetsedwa kwanu, panthawi imene
magulu awiri adakumana, kudalamulidwa ndi Mulungu
ndi cholinga chakuti akhoza kuyesa anthu okhulupirira.
167. Ndipo kuti ayese anthu achinyengo ndipo iwo auzidwa
kuti: "Bwerani kuti mumenye nkhondo mu njira ya
Mulungu kapena kuti mudziteteze inu nokha." Iwo adati:
"Ngati ife tikadadziwa kuti kukhala nkhondo, ndithudi
Ife tikadapita nanu." Patsiku limeneli kusakhulupirira
kwawo kudawayandikira kuposa chikhulupiriro. Iwo anali

kunena ndi milomo yawo zinthu zomwe sizinali m'mitima
yawo. Ndipo Mulungu amadziwa zimene iwo anali kubisa.
168. Iwo ndi amene adanena za abale awo amene anafa pamene
iwo anakhala osapita ku nkhondo: Iwo akadatimvera ife,
sakadaphedwa ayi. Nena: "Dzichotsereni imfa imene ili
pakati panu ngati zimene munena ndi zoona."
169. Inu musaganize kuti amene adaphedwa m'njira ya
Mulungu adafa ayi. Iyayi, koma iwo ali ndi moyo ndipo
amasamalidwa ndi Ambuye wawo ndipo ali ndi gawo
lawo. 170. Iwo amasangalala chifukwa cha zimene Mulungu
wawapatsa mwa chisomo chake ndi chifukwa cha iwo
amene sadalowe mgulu lawo ndipo anatsala m'mbuyo,
ndipo iwo sadzakhala ndi mantha kapena kumva chisoni.
171. Iwo amasangalala ndi chisomo ndi chuma chochokera
kwa Mulungu ndipo kuti Mulungu sadzaononga malipiro
a okhulupirira. 172. Iwo amene adavomera kuitana kwa
Mulungu ndi Mtumwi pamene atavulala ndi iwo amene
amachita ntchito zabwino ndi kuopa Mulungu, adzalandira
mphotho ya mtengo wapatali. 173. Iwo amene anthu adati
kwa iwo: "Ndithudi anthu asonkhanitsidwa kuti alimbane
nanu, motero chitani mantha." Koma izi zidangoonjezera
chikhulupiriro chawo ndipo iwo adati: "Chithandizo
cha Mulungu ndi chokwanira kwa ife chifukwa Iye
ndiye Mtetezi wabwino." 174. Ndipo iwo adabwerera ndi
chisomo ndi zokoma zake za Mulungu. Ndipo padalibe
choipa chimene chidawagwera iwo. Ndipo iwo adatsatira
zomukondweretsa Mulungu. Ndipo Mulungu ndiye
Mwini wa zokoma zazikulu zosatha. 175. Ndi Satana
amene amakupangitsani kuti inu muziopa omutsatira

ake. Musawaope iwo koma ndiopeni Ine ngati inu ndinu
okhulupirira.
176. Ndipo asakukhumudwitseni anthu amene amachita
changu posakhulupirira. Ndithudi iwo sangachite chili
chonse chomupweteka Mulungu. Ndi cholinga cha
Mulungu kuti iwo asadzapatsidwe gawo lina lililonse
m'moyo umene uli nkudza. Iwo ali ndi chilango chachikulu.
177. Ndithudi iwo amene amasinthitsa chikhulupiriro chawo
posankha kusakhulupirira sadzachita china chili chonse
chopweteka Mulungu ayi. Ndipo chilango chowawa
chidzakhala pa iwo. 178. Ndipo anthu osakhulupirira
asaganize kuti Ife tili kuchedwetsa chilango chawo ndi
cholinga chabwino kwa iwo. Ife tili kuchichedwetsa ndi
cholinga chakuti apitilize kulakwa. Chilango chochititsa
manyazi chili kuwayembekezera. 179. Mulungu sadzawasiya
anthu okhulupirira m'mavuto amene muli nawo tsopano
mpaka pamene Iye asiyanitsa oipa pakati pa abwino. Ndipo
Mulungu sadzakuululilani zinthu zobisika, koma Mulungu
amasankha Atumwi ake amene Iye wawafuna. Kotero
khulupiririrani mwa Mulungu ndi Atumwi ake. Ndipo ngati
inu mukhulupirira ndi kuopa Mulungu, mudzakhala ndi
malipiro akulu.
180. Ndipo anthu oumira, amene safuna kupereka
gawo lina limene Mulungu wawapatsa kuchokera ku
chuma chake, asaganize kuti ali kuchita zabwino. Iyayi,
zidzawavuta. Zinthu zimene amabisa zidzamangidwa
m'makosi mwawo patsiku louka kwa akufa. Mulungu
ndiye mwini wa chilichonse chimene chili mlengalenga
ndi padziko lapansi ndipo Mulungu amadziwa chilichonse
chimene mumachita. 181. Ndithudi Mulungu wamva mawu

a iwo amene adati: “Ndithudi Mulungu ndi osauka koma ife
ndife olemera.” Ife tidzalemba zomwe amanena ndi kupha
kwawo kwa Atumwi opanda chifukwa ndipo Ife tidzanena
kuti: “Lawani chilango chanu cha moto wowotcha.” 182. Ichi
ndi chifukwa cha zimene manja anu adatsogoza. Ndipo
ndithudi Mulungu sapondereza akapolo ake. 183. Iwo amene
adati: “Ndithudi Mulungu adavomera lonjezo lathu loti
tisakhulupirire mwa Mtumwi wina aliyense pokhapokha
ngati iye atibweretsera nsembe yomwe idzawotchedwa ndi
moto wochokera kumwamba.” Nena: “Ndithudi! Kudadza
kwa inu Atumwi ena ine ndisanadze ndi zizindikiro zooneka
ndi zina za zimene mwanenazi. Kodi ndi chifukwa chiyani
mudawapha awa ngati zimene muli kunena ndi zoona?”
184. Ngati iwo akukana iwe, Atumwi ena adakanidwanso iwe
usanadze, amene adabweretsa zizindikiro zooneka, Mau a
Mulungu ndi Buku loonetsa chilangizo. 185. Mzimu uliwonse
udzalawa imfa. Inu mudzalandira malipiro anu patsiku la
kuuka kwa akufa. Ndipo aliyense amene adzapulumutsidwa
ku moto ndi kulowa ku Paradiso, ndithudi, iye adzakhala
opambana. Moyo wa padziko lapansi si wina uliwonse
koma ka mtendere ka nthawi kochepa.

186. Ndithudi inu mudzayesedwa mu chuma chanu ndi inu
eni, ake ndipo inu mudzamva zonyansa zambiri kuchokera
kwa anthu amene adapatsidwa Buku inu musadadze ndi
kuchokera kwa iwo amene amafanizira Mulungu ndi
zinthu zina. Koma ngati mupirira ndi kumuopa Mulungu,
ndithudi, zimenezo ndizo zofunikira kuchita. 187. Ndi
pamene Mulungu adachita chipangano ndi iwo amene
analandira Buku kale, kuti: “Alalikire Mau kwa anthu a
mitundu yonse mosabisa ayi.” Koma iwo adaponya Mau

a Mulungu kumbuyo kwawo ndi kugula zinthu zopanda
pake. Ndithudi zoipa zokha ndizo zimene iwo adagula.
188. Musaganize kuti iwo amene amasangalala ndi zimene
achita ndiponso iwo amene amafuna kuyamikidwa pa
zinthu zimene iwo sanachite, kuti adzathawa chilango
chathu, ndipo chilango chowawa chiri kuwadikira.
189. Mwini Ufumu wa kumwamba ndi wa padziko lapansi
ndi Mulungu. Mulungu ali ndi mphamvu pa zinthu zonse.
190. Ndithudi! Muchilengedwe chakumwamba ndi
dziko lapansi ndi m'kasinthidwe ka usiku ndi usana,
ndithudi muli zizindikiro kwa anthu anzeru. 191. Iwo
amene amakumbukira Mulungu ataimirira, atakhala
pansi ndi pamene agona cham'mbali ndipo amaganiza
m'zachilengedwe chakumwamba ndi dziko lapansi;
namati: "Ambuye wathu! Inu simudalenge izi wopanda
cholinga ayi. Ulemerero ukhale kwa Inu! Tipulumutseni
ife ku mazunzo a ku moto." 192. "Ambuye wathu! Ndithudi
yense amene Inu mudzamuponya ku Moto, ndithudi,
wotero adzachititsidwa manyazi ndipo anthu ochita zoipa
sadzapeza owathandiza." 193. "Ambuye wathu! Ndithudi ife
tamva kuitana kwa iye amene ali kuwaitana anthu kuti adze
ku chipembedzo choonadi." Iye adati: "Khulupirirani mwa
Ambuye wanu ndipo ife takhulupirira. Ambuye wathu
tikhululukireni ife machimo athu ndipo chotsani kwa ife
ntchito zathu zoipa ndipo tipangeni kuti tife pamodzi
ndi anthu olungama." 194. "Ambuye wathu! Tipatseni ife
zimene mudatilonjeza kudzera mwa Atumwi anu ndipo
musadzatichititse manyazi ife pa tsiku la kuuka kwa akufa
chifukwa Inu simuphwanya lonjezo."
195. Motero Ambuye wawo adavomera pemphero lawo

nati: “Ine sindidzaononga mphoto ya ntchito za munthu
wa mwamuna kapena wa mkazi amene ali pakati panu.” Inu
ndinu amodzi. Iwo amene adasamuka m’nyumba zawo ndi
kupirikitsidwa kuchoka mu izo ndi kuzunzidwa mu njira
yanga ndi iwo amene adamenya nkhondo ndi kuphedwa
mnjira yanga, ndithudi, Ine ndidzawakhululukira machimo
awo ndipo ndidzawalowetsa ku minda yothiriridwa
ndi madzi a m’mitsinje yoyenda pansi pake, mphatso
yochokera kwa Mulungu. Ndipo kwa Mulungu ndiye
kumene kuli malipiro abwino. 196. Inu musanyengedwe ndi
makhalidwe a anthu osakhulupirira pa dziko lonse lapansi.
197. Kupeza bwino kwawo ndi kwa kanthawi kochepa
ndipo Gahena ndiyo idzakhala mudzi wawo, malo onyansa
kukhalamo. 198. Koma iwo amene amaopa Mulungu, kuli
minda yothiriridwa ndi madzi woyenda pansi pake kumene
adzakhalako mpaka kalekale, chisangalalo chochokera kwa
Ambuye wawo. Ndithudi chimene chili ndi Mulungu ndi
chabwino kwa anthu olungama. 199. Ndipo, ndithudi, alipo
anthu ena pakati pa anthu a m’Buku amene amakhulupirira
mwa Mulungu ndi zimene zavumbulutsidwa kwa inu ndi
kwa iwo ndipo amadzichepetsa pamaso pa Mulungu.
Ndipo iwo sagulitsa chivumbulutso chake pamtengo
wochepa ndipo malipiro awo ali kwa Ambuye wawo.
Ndithudi Mulungu ndi wachangu powerengera. 200. Oh
inu anthu okhulupirira! Pilirani ndipo khalani opirira
kwambiri ndipo tetezani dziko lanu poika Asirikari pamalo
okhazikika pamene adani anu akhoza kudzera, ndipo
muope Mulungu kuti mukhoza kukhala opambana.

# Al Nisa

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Oh inu anthu! Muopeni Ambuye wanu amene
anakulengani inu kuchokera kwa munthu mmodzi ndipo
kuchokera kwa munthu ameneyu, Iye analenga mkazi
wake. Ndipo kudzera mwa iwo, Iye adadzadza dziko lonse
lapansi ndi anthu amuna ndi akazi osawerengeka. Opani
Mulungu, dzina limene mumadandaulirana wina ndi
mnzake. Ndipo lemekezani chibale. Ndithudi Mulungu
amakuyang'anirani nthawi zonse. 2. Apatseni ana a masiye
chuma chawo akafika msinkhu woyenera. Musasinthitse
choipa ndi chabwino ndipo musadye chuma chawo
pamodzi ndi chanu chifukwa kutero, ndithudi, ndi tchimo
lalikulu. 3. Ngati inu muopa kuti simungathe kuchita
chilungamo ndi ana a masiye, kwatirani mkazi amene
mungamukonde awiri, atatu kapena anayi. Koma ngati inu
muopa kuti simudzatha kuchita chilungamo, kukwaniritsa
zonse bwinobwino, kwatirani mmodzi yekha kapena wina
wa a kapolo a chitsikana amene muli nawo. Chimenechi
chidzakhala chapafupi kwa inu kuti musalephere kutsata
njira ya chilungamo. 4. Apatseni akazi mphatso yawo
monga mphatso yaulere. Koma ngati iwo, mwa chifuniro
chawo, asankha kukugawiraniko gawo la mphatsoyi, idyani
mosangalala ndi mwa ubwino.

5. Musawapatse anthu ozerezeka katundu amene

Mulungu wakupatsani kuti muziwathandizira, koma
inu muyenera kuwasamala ndi kuwaveka kuchokera
ku phindu la katunduyu ndipo lankhulani nawo mawu
abwino a chifundo. 6. Aikeni ana a masiye pa mayesero
mpakana pamene afika poti atha msinkhu. Ngati inu
muona kuti ndi a maganizo okhazikika, apatseni chuma
chawo ndipo musawaonongere iwo chuma chawo asanathe
msinkhu. Munthu amene ali olemera asagwiritse ntchito
katundu wa ana a masiye amene ali kumuyang'anira ndipo
munthu osauka agwiritse ntchito chuma cha ana a masiye
mosamala ndi mwa chilungamo. Pamene inu muwapatsa
chuma chawo, itanani ena kuti akhale mboni; Mulungu
ndi wokwana kukhala mboni pa zonse zimene muchita.
7. Amuna adzakhala ndi gawo mu katundu amene makolo
ndi abale awo asiya ndipo akazi adzakhala ndi gawo mu
katundu amene makolo ndi abale awo asiya. Kaya katunduyo
ndi wochepa kapena wambiri, onse ayenera kulandira
gawo lawo malinga ndi malamulo. 8. Ngati a chibale, a
masiye kapena osauka alipo pamene ali kugawa chuma cha
masiye, agawireniko nawonso ndipo alankhuleni ndi mawu
abwino. 9. Alekeni iwo amene amafunira zabwino ana
awo, pamene iwo akufa, kuti asamale posawalakwira ana
amasiye. Alekeni kuti aope Mulungu ndi kunena zinthu
zokhazikitsa choonadi. 10. Kwa iwo amene amadya chuma
cha ana a masiye mopanda chilungamo amameza moto
m'mimba mwawo ndipo iwo adzalowa m'malawi a moto wa
ku Gahena.

11. Mulungu wakulamulirani motere pankhani za ana
anu: Mwana wa mwamuma adzalandira magawo awiri
kuposa mwana wa mkazi. Ndipo ngati ana a akazi apitirira

awiri, iwo adzalandira magawo awiri pa magawo atatu a katundu wosiyidwa koma ngati alipo mwana mmodzi yekha wamkazi, adzalandila theka ndipo makolo ake awiri, aliyense mwa iwo adzalandira gawo limodzi la magawo asanu ndi limodzi – muzimene adasiya malemuyo ngati malemuyo ali ndi mwana. Koma ngati alibe mwana ndipo makolo ake ndiwo amene ayenera kulandira katundu wake, amayi ake adzalandira gawo limodzi la magawo atatu. Ngati iye ali ndi abale ake, amayi ake adzalandira gawo limodzi la magawo asanu ndi limodzi atatha kukwaniritsa lonjezo la malemu ndiponso kubweza ngongole. Inu simudziwa kuti pakati pa makolo anu ndi ana anu amene ali wa phindu ndi inu. Ili ndi lamulo la Mulungu. Ndithudi Mulungu ndi wanzeru ndi wodziwa chilichonse. 12. Inu mudzalandira theka la chuma chimene akazi anu adasiya, ngati iwo alibe mwana. Ngati ali ndi mwana, inu mudzalandira gawo limodzi la magawo anayi la zimene mkaziyo wasiya pambuyo popereka zimene analonjeza ndi kubwezera ngongole. Nawo akazi anu adzapeza gawo limodzi m'magawo anayi muzimene mwasiya ngati mulibe mwana. Koma ngati muli ndi mwana, iwo, akaziwo, adzapeza gawo limodzi la magawo asanu ndi atatu a zimene mwasiya, pambuyo popereka zimene mudalonjeza ndi kubwezera ngongole. Ngati mwamuna kapena mkazi ndi yemwe wasiya katundu ndipo alibe mwana kapena mdzukulu, koma ali ndi mchimwene wake kapena mchemwali wake, aliyense wa iwo adzapeza gawo limodzi m'magawo asanu ndi limodzi, ndipo ngati adali ambiri koposa apo adzagawana gawo limodzi la magawo atatu pambuyo popereka zimene analonjeza kapena kubwezera ngongole

mosabweretsa mavuto. Limeneli ndi lamulo lochokera
kwa Mulungu, Mulungu ndi wodziwa ndi woleza mtima.
13. Awa ndi malire a Mulungu. Ndipo aliyense amene
amvera Mulungu ndi Mtumwi wake adzaikidwa m'minda
yoyenda mitsinje pansi pake kumene adzakhalako nthawi
zonse. Ndipo kumeneko ndiko kupambana kwakukulu. 14.
Koma iye amene amanyoza Mulungu ndi Mtumwi wake
ndipo amalumpha malire ake, adzamuponya ku moto wa
ku Gahena ndipo adzakhala komweko mpaka kalekale
ndipo iye adzalandira chilango chochititsa manyazi.

15. Ndipo iwo, mwa akazi anu, amene achita chigololo,
pezani mboni zokwanira zinayi zochokera pakati panu
ndipo ngati iwo apereka umboni wotsimikiza, asungeni
kunyumba zawo mpaka pamene imfa iwapeza kapena
mpaka pamene Mulungu alamula kwa iwo njira ina.
16. Ndipo ngati anthu awiri achita chigololo pakati panu,
alangeni onse awiri. Ngati iwo alapa ndi kusiya njira zawo
zoipa, asiyeni. Ndithudi Mulungu ndi wokhululukira ndi
wa chisoni chosatha. 17. Mulungu amavomera kulapa kwa
amene achita zoipa mosazindikira ngati alapa mwamsanga.
Ndi iwo amene Mulungu adzawakhululukira ndipo
Mulungu ndi wodziwa ndiponso wanzeru. 18. Kulibe phindu
kulapa kwa iwo amene amachita zinthu zoipa mpaka
pamene imfa imupeza wina wa iwo ndipo ati: "Tsopano
ndalapa," kapena kwa iwo amene amafa ali osakhulupirira.
Kwa iwo Ife tawakonzera chilango chowawa.

19. Oh inu anthu okhulupirira! Inu simuloledwa
kulowa chokolo chokakamiza ndipo musawazunze ndi
cholinga choti muwalande zina zimene mudawapatsa
pokhapokha ngati achita chigololo. Ndipo khalani

nawo mwa mtendere. Ngati simukuwafuna, mwina
mungachide chinthu chimene Mulungu waikamo zabwino
zambiri. 20. Koma ngati inu mufuna kusudzula mkazi
ndi cholinga chokwatira mkazi wina ndipo mutampatsa
mmodzi mwa iwo chuma chochuluka, ngati mphatso ya
ukwati, musatenge chilichonse mwa chumacho. Kodi
inu mungakhale mopanda chilungamo ndikuwonetsa
kuchimwa poyera? 21. Kodi inu mungalande bwanji chuma
pamene munali kugonera limodzi, ndipo iwo adakupatsani
chipangano chotsimikizika? 22. Ndipo musakwatire mkazi
amene adakwatiwapo ndi abambo anu, kupatula zimene
zidatha kale. Ndithudi zinali zochititsa manyazi; zonyansa
ndiponso njira yauchimo.

23. Inu mwaletsedwa kukwatira awa: Amayi anu, ana anu
a akazi, alongo anu, azakhali anu, achemwali amayi anu,
ana akazi achimwene anu, ana akazi a alongo anu, amayi
amene adakuyamwitsani, akazi amene mudayamwitsidwa
nawo bere limodzi, apongozi anu, ndi ana a akazi owapeza
amene muli kuwasunga amene anabereka akazi amene
mwawakwatira. Koma ngati simunagonepo ndi amai
awo palibe choletsa kwa inu kuwakwatira atsikanawo.
Kukwatira akazi a ana anu amuna amene mudabereka inu ndi
akazi awiri amimba imodzi nthawi imodzi ndi koletsedwa
kupatula zimene zinachitika kale. Ndithudi Mulungu
ndi okhululukira ndi wa chisoni chosatha. 24. Ndipo
ndikoletsedwa kukwatira akazi okwatiwa kupatula amene
ali m'manja mwanu ngati akapolo. Limeneli ndi lamulo la
Mulungu kwa inu. Ndipo ndi kololedwa kwa inu kukwatira
wina aliyense amene sanatchulidwe pamwambapa
ngati inu muwapatsa mphatso ya ukwati kuchokera ku

chuma chanu mu njira yabwino osati ya chiwerewere. Amene muwakwatira , apatseni mphatso yawo ya ukwati motsatira malamulo. Koma pamene mphatso itchulidwa, sizolakwika kwa inu ngati mugwirizana. Ndithudi Mulungu ndi wodziwa, ndi Waluntha.
25. Ndipo ngati wina wa inu alibe mwayi woti nkukwatira mkazi wokhulupirira amene ndi mfulu, mukhoza kukwatira mwa atsikana anu wokhulupirira kuchokera kugulu la akapolo amene muli nawo, ndipo Mulungu amadziwa zonse za chikhulupiriro chanu ndipo inu ndinu amodzi. Akwatitseni ndi chilolezo cha ambuye awo ndipo muwapatse mphatso yawo ya ukwati mwa chilungamo. Iwo ayenera kudzisunga, osati a chiwerewere kapena wochita chibwenzi. Ndipo ngati akwatiwa ndipo achita chigololo, chilango chawo ndi theka la chilango chimene mfulu ya ikazi ingalandire. Ichi chikhudza iye amene aopa kupwetekeka pakati pa inu. Koma ndi kwabwino ngati inu mudziletsa ndipo Mulungu ndi wokhululukira ndi Mwini chisoni chosatha.

26. Mulungu afuna kuti akufotokozereni inu ndi kukutsogolerani ku njira za iwo amene adalipo inu musanadze ndi kukukhululukirani inu. Ndipo Mulungu ndi wodziwa ndi wanzeru.
27. Mulungu afuna kukukhululukirani inu koma iwo amene amatsatira zilakolako zawo amafunisitsa mutasiya njira yoyenera.
28. Mulungu afuna kukupeputsirani malamulo ake chifukwa munthu analengedwa wofoka.

29. Oh inu anthu okhulupirira! Musadye chuma cha anzanu mopanda chilungamo ngakhale kuti ndi malonda amene mwagwirizana pakati panu. Ndipo musawonongane wina ndi mzake. Ndithudi Mulungu ndi wa chifundo

chosatha kwa inu. 30. Ndipo aliyense amene achita
izi mwamtopola kapena mwakusowa chilungamo, Ife
tidzamulowetsa kumoto ndipo kutero si chinthu chovuta
kwa Mulungu. 31. Ngati inu mupewa machimo akuluakulu
amene mukuletsedwa, Ife tidzakukhululukirani machimo
anu ndipo tidzakulowetsani kukhomo lolemekezeka.
32. Ndipo musasirire zokoma zimene Mulungu wawapatsa
ena a inu kuposa anzawo. Kwa amuna kuli gawo kuzimene
amachita, nawonso akazi ali ndi gawo muzimene amachita
ndipo mupempheni Mulungu kuti akupatseni zabwino
zake. Ndithudi Mulungu amadziwa chinthu chilichonse.
33. Ndipo kwa aliyense tamuikira abale olandira chuma
chimene chasiyidwa ndi makolo ndi abale. Ndipo iwo
amene mwachita nawo chipangano, apatseni gawo lawo
nawonso kuti alandire. Ndithudi Mulungu ndi mboni pa
zinthu zonse.

34. Anthu amuna ndi atetezi ndi osamala anthu akazi
chifukwa Mulungu wawalemekeza ena kuposa anzawo
ndiponso chifukwa cha chuma chawo chimene amagwiritsa
ntchito. Motero akazi ochita zabwino ndipo amene
amamvera, amasunga pamene amuna awo palibe, ndi
zimene Mulungu awalamulira kuti azisunge. Ndipo akazi
amene mukuona kuti samvera achenjezeni ndipo ngati
iwo sasintha asiyeni agone pa okha ndipo ngati sasinthabe
amenyeni. Koma ngati iwo akumverani, musawafunire
njira yachabe. Ndithudi Mulungu ndi wapamwamba ndi
wamkulu. 35. Ndipo ngati inu muopa kuti asiyana, sankhani
nkhoswe kuchokera kwa m'bale wa mwamuna ndiponso
nkhoswe kuchokera kwa m'bale wa mkazi ngati iwo akufuna

kuyanjanitsidwa, ndipo Mulungu adzawayanjanitsa pakati
pawo. Ndithudi Mulungu ndi wodziwa ndi wozindikira.
36. Pembedzani Mulungu ndipo musamuphatikize Iye
ndi china chilichonse ndipo chitani zabwino kwa makolo
anu ndi achibale, kwa a masiye ndi kwa osauka, ndi kwa
anzanu amene muli nawo pafupi kapena kutali ndi anzanu
okhala nawo pafupi, ndi kwa a paulendo ndi kwa akapolo
anu. Ndithudi Mulungu sakonda anthu a mtudzu ndi
odzikundikira. 37. Iwo amene ndi oumira ndipo amauza
anzawo kuti akhalenso oumira, amene amabisa chuma
chimene Mulungu adawapatsa mwachifundo chake.
Ndipo Ife tawakonzera anthu osakhulupirira chilango
chochititsa manyazi. 38. Ndi iwo amene amaononga chuma
chawo modzionetsera kwa anthu, ndipo sakhulupirira
mwa Mulungu ndi tsiku la chiweruzo; ndipo aliyense
amene asankha Satana kukhala bwenzi lake, wasankha
bwenzi loopsya. 39. Kodi iwo akadataya chiyani ngati
akadakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku la chiweruzo ndi
kupereka muzinthu zimene Mulungu adawapatsa iwo kuti
ziziwathandiza? Mulungu amawadziwa onse. 40. Ndithudi!
Mulungu sapondereza malipiro ngakhale a kanthu kochepa,
ndipo ngati muli zabwino Iye adzakaonjezera malipiro ake
ndipo amapereka kuchokera kwa Iye malipiro ochuluka.
41. Kodi zidzakhala bwanji pamene tidzabweretsa
mboni kuchokera ku anthu a mtundu uliwonse ndipo
tikubweretsa iwe kuti uzakhale mboni yowatsutsa?
42. Patsikulo onse amene sadakhulupilire ndipo sanamvere
Mtumwi adzafunitsitsa akadaundiridwa m'nthaka koma
iwo sadzabisa china chilichonse kwa Mulungu. 43. Oh inu
anthu okhulupirira! Musayandikire mapemphero pamene

muli oledzera mpaka pamene mudziwa tanthauzo la zimene
muli nkunena ndiponso pamene mwakhala malo ndi a
kunyumba kwanu ndipo simunasambe kupatula pamene
muli pa ulendo. Ndipo ngati muli nkudwala kapena muli pa
ulendo kapena mmodzi mwa inu wachokera ku chimbudzi
kapena mwagona limodzi ndi akazi anu, ndipo simudapeze
madzi, tapani dothi labwino ndipo mupukute nkhope
ndi manja anu. Ndithudi Mulungu ndi wa chifundo ndi
okhululukira.
44. Kodi iwe siunawaone iwo amene adapatsidwa gawo
la Buku ali kusochera ndipo akufuna kuti iwe usochere ku
njira yabwino? 45. Mulungu amawadziwa bwino adani anu
ndipo Mulungu ndi wokwana kukhala Mtetezi ndipo ndi
wokwana kukhala Mthandizi. 46. Pakati pa Ayuda pali ena
amene amasinthitsa mawu m'malo mwake ndipo amati: "Ife
tamva mau ako koma sitikumvera ndipo imva koma usamve
chili chonse" ndipo amati: 'Chenjera, timvere ife ndipo ife
tidzakumvera' ali kupotoza malirime awo ndi cholinga
chotukwana chipembedzo. Koma iwo akadati: "Tamva
ndipo tatsatira; tiphunzitse ife"; zikadawakhalira bwino
kwambiri, koma Mulungu wawatemberera iwo chifukwa
chosakhulupirira kwawo motero iwo sakhulupilira koma
pang'ono.
47. Oh inu anthu amene mudapatsidwa Buku!
Khulupiriráni zimene tavumbulutsa zimene zitsimikizira
Mau a Mulungu amene muli nawo, tisadatembenuze nkhope
ndikuzibwezera kumbuyo kwake kapena kuwatemberera
monga mmene tidawatemberera anthu ophwanya tsiku
la Sabata. Ndipo lamulo la Mulungu limatsatidwa ndipo
limakwaniritsidwa! 48. Ndithudi Mulungu sakhululukira

kuti milungu izipembedzedwa yowonjezera pa Iye koma
Iye amakhululukira aliyense amene wamufuna pa machimo
ena. Ndipo aliyense amene amapembedza milungu ina
yowonjezera pa Iye, iye, ndithudi, wapeka bodza loopsya.
49. Kodi simunaone amene amadziyeretsa okha? Iyayi!
Koma Mulungu amayeretsa aliyense amene Iye wamufuna
ndipo iwo sadzaponderezedwa ngakhale ndi pang'ono
pomwe. 50. Taona mmene iwo amapekera bodza lokhudza
Mulungu ndipo zimenezi zikukwanira kukhala tchimo
looneka.
51. Kodi siunaone iwo amene adapatsidwa gawo la
Buku la Mulungu? Iwo amakhulupirira mafano ndi
milungu yabodza ndipo amawauza osakhulupilira kuti
ndi otsogozedwa bwino kuposa anthu okhulupirira.
52. Amenewa ndiwo anthu amene Mulungu wawatemberera
ndipo aliyense amene atembereredwa ndi Mulungu iwe
siungamupezere womuthandiza. 53. Kodi kapena iwo ali
ndi gawo mu Ufumu? Zikadatero, iwo sakadawapatsa
anthu ngakhale kanthu kakang'ono. 54. Kodi kapena iwo
amachitira kaduka anthu mu zinthu zabwino zimene
Mulungu wawapatsa? Ife tidawapatsa ana a Abrahamu
Buku ndi luntha ndipo tidawapatsa Ufumu waukulu. 55. Ena
mwa iwo adakhulupirira iye koma ena a iwo anayang'ana
kumbali ndipo Moto ukukwanira kukhala chilango
chawo. 56. Ndithudi iwo amene adakana zizindikiro zathu
tidzawaotcha ku moto. Nthawi zonse pamene makungu
awo azidzapsya, Ife tidzawapatsa makungu ena kuti iwo
alawe chilango. Ndithudi Mulungu ndi wamphamvu nthawi
zonse ndi Wanzeru. 57. Koma iwo amene amakhulupirira
ndi kuchita ntchito zabwino, Ife tidzawalowetsa m'minda

yothiriridwa ndi mitsinje yoyenda pansi pake, ndipo
adzakhalako mpaka kalekale. Ndipo kumeneko adzakhala
ndi akazi oyera ndipo Ife tidzawalowetsa ku mthunzi
wabwino kwambiri.
58. Ndithudi Mulungu ali kukulamulirani kuti mubwezere
katundu amene mwasunga kwa eni ake ndipo ngati
muweruza pakati pa anthu, weruzani mwachilungamo.
Ndithudi chilangizo chimene Mulungu akukulangizani
ndi chabwino kwambiri. Ndithudi Mulungu amamva
nthawi zonse ndipo amaona zinthu zonse. 59. Oh inu anthu
okhulupirira! Mverani Mulungu ndipo mverani Mtumwi
wake ndiponso iwo amene ali ndi udindo pakati panu.
Ndipo ngati mutsutsana pa chinthu china chilichonse,
chiperekeni icho kwa Mulungu ndi Mtumwi wake ngati
inu mumakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza.
Zimenezi zidzakhala zabwino ndi zolungama pomaliza.
60. Kodi iwe wawaona amene amanena kuti amakhulupirira
mu zimene zavumbulitsidwa kwa iwe ndi kwa Atumwi
ena amene adalipo iwe usanadze ndipo iwo amafunafuna
chiweruzo cha oweruza abodza, pamene iwo adalamulidwa
kuti awakane iwo? Koma chofuna cha Satana ndi
kuwasokeretsa iwo ku njira yoyenera. 61. Ndipo pamene
auzidwa "Bwerani ku zimene Mulungu wavumbulutsa
ndiponso kwa Mtumwi," iwe umaona anthu a chinyengo ali
kukukana iwe mwamwano. 62. Kodi bwanji, ngati vuto ligwa
pa iwo chifukwa cha ntchito zimene adatsogoza manja awo,
amadza kwa iwe, kulumbira m'dzina la Mulungu kuti: "Ife
sitifuna china chilichonse koma zabwino ndi chigwirizano!"
63. Awa ndiwo amene Mulungu amadziwa zimene zili

m'mitima mwawo. Motero asiye koma uwachenjeze ndipo
uwauze mawu ogwira mtima.

64. Ifesitidatumize Mtumwi aliyense, koma kuti atsatiridwe
mwa lamulo la Mulungu. Ngati iwo adadzilakwitsa,
akanadza kwa iwe kupempha chikhululukiro cha Mulungu
ndipo Mtumwi akadawapemphera chikhululukiro cha
Mulungu. Iwo akadamupeza Iye wokhululuka ndi wa
chisoni. 65. Koma iyayi, pali Ambuye wako, iwo sadzakhala
okhulupirira mpaka pamene akusankha iwe kukhala
oweruza pa mikangano ya pakati pawo ndipo satsutsa
chiweruzo chako, ndipo achivomeleza kwathunthu.
66. Zikadakhala kuti Ife tidawalamulira kuti: "Mudziphe
nokha kapena tulukani m'nyumba zanu," sakadachita
kupatula owerengeka okha. Koma ngati iwo akadachita
zimene auzidwa zikadakhala bwino kwa iwo, ndipo
zikadaonjezera chikhulupiriro 67. Ndipo ndithudi Ife
tikadawapatsa iwo, kuchokera kwa Ife, dipo lalikulu.
68. Ndithudi Ife tikadawatsogolera ku njira yoyenera.
69. Ndipo aliyense amene amvera Mulungu ndi Mtumwi
wake, ameneyo ndi amene ali pamodzi ndi anthu amene
Mulungu wawadalitsa kuchokera ku gulu la Atumwi,
anthu a chilungamo, anthu ofera ku nkhondo m'njira ya
Mulungu ndi anthu ochita zabwino. Ati bwanji kukoma
kukhala mgulu lotere? 70. Ichi ndi chisomo chochokera kwa
Mulungu, ndipo Mulungu ndi wokwanira kukhala wodziwa
chili chonse.

71. Oh inu anthu okhulupirira! Khalani okonzeka ndipo
yendani m'magulu m'magulu kapena pa gulu limodzi lokha.
72. Alipo wina pakati panu amene adzatsalira m'mbuyo.
Amene ngati choipa chioneka kwa inu amanena kuti:

“Ndithudi Mulungu wandionetsera ine chifundo chifukwa sindinali nawo.” 73. Koma ngati mtendere wochokera kwa Mulungu ukupezani, ndithudi iye adzanena ngati kuti padalibe ubwenzi pakati pa iye ndi inu ndipo iwo adzati: “Ndikadakhala nawo limodzi, ndithudi ndikadakhala ndi mwayi waukulu.” 74. Kotero alekeni iwo amene amagulitsa moyo uno ndi moyo umene uli nkudza kuti amenye nkhondo mu njira ya Mulungu. Aliyense amene amenya nkhondo m’njira ya Mulungu ndipo aphedwa kapena apambana, Ife tidzamupatsa dipo lalikulu. 75. Kodi ndi chifukwa chiyani inu simukumenya nkhondo m’njira ya Mulungu pamene anthu ofoka mwa anthu amuna, akazi ndi ana amati: “Ambuye wathu! Tipulumutseni kuchoka kumzinda uwu wa anthu wochita zoipa ndipo tidzutsireni mtetezi wochokera kwa Inu amene adzatithandiza ife.” 76. Iwo amene akhulupirira amamenya nkhondo m’njira ya Mulungu koma amene sakhulupilira amamenya mu njira ya Satana. Kotero inu menyanani ndi abwenzi a Satana, ndithudi chikonzero cha Satana ndi chopanda mphamvu.

77. Kodi siunaone anthu amene amauzidwa kuti: “Musamenye nkhondo, pempherani mwandondomeko ndipo perekani msonkho wothandizira anthu osauka,” koma pamene iwo adalamulidwa kuti amenye nkhondo, taona; ena a iwo amaopa anthu monga momwe amamuopera Mulungu kapenanso kuposa apa. Iwo amati: “Ambuye wathu! Kodi ndi chifukwa chiyani mwatilamula kuti timenye nkhondo? Kodi simungatipatse nthawi yopumula ngakhale yochepa” Nena: “Chisangalalo cha moyo uno ndi chochepa kwambiri. Moyo umene uli nkudza ndi wabwino kwambiri kwa iye amene amaopa Mulungu ndipo

inu simudzaponderezedwa ndi pang'onong'ono pomwe."
78. Pali ponse pomwe mungakhale, imfa idzakupezani,
ngakhale inu mutadzitsekera mkati mwa nsanja zolimba.
Ndipo ngati zabwino ziwapeza, iwo amati: "Izi zachokera
kwa Mulungu" koma ngati choipa chiwagwera, iwo
amati: "Ichi ndi chochokera kwa iwe." Nena: "Zinthu
zonse zimachokera kwa Mulungu." Kodi ndi chiani
chawapeza anthu awa kuti sangathe kuzindikira china
chiri chonse? 79. Chilichonse chabwino chimene chidza pa
iwe ndi chochokera kwa Mulungu, ndipo choipa chimene
chikupeza ndi chochokera kwa iwe mwini. Ndipo Ife
takutumiza iwe ngati Mtumwi kwa anthu onse. Ndipo
Mulungu akwana kukhala mboni.
80. Aliyense amene amvera Mtumwi ndithudi amvera
Mulungu ndipo iye amene safuna kukumvera iwe, Ife
sitidakutumize kuti ukhale wowayang'anira ayi. 81. Iwo
amati: "Ife ndife omvera" koma iwo akangochoka kwa iwe,
ambiri a iwo amachita chiwembu usiku pochita zinthu
zimene siukunena. Koma Mulungu amalemba ziwembu
zawo zonse zomwe amachita usiku. Kotero aleke okha
ndipo ika chikhulupiliro chako mwa Mulungu. Ndipo
Mulungu ndi okwana kukhala Mtetezi. 82. Kodi iwo
salingalira za Korani? Ilo likadakhala kuti silinachokere kwa
Mulungu, iwo akadapeza mu ilo kusemphana kwambiri.
83. Pamene iwo amva nkhani iliyonse ya mtendere kapena
yochititsa mantha, iwo amaiulutsa koma iwo akanaipereka
kwa Mtumwi kapena kwa amene ali ndi udindo pakati
pawo kapena anthu amene amafufuza bwino nkhani,
akadadziwa. Ndipo pakadapanda chisomo ndi chisoni cha

Mulungu pa inu, inu mukanatsatira Satana kupatula anthu
ochepa okha.
84. Motero menya nkhondo mu njira ya Mulungu, iwe
siudzafunsidwa za munthu wina ayi koma za iwe wekha
ndipo alimbikitse okhulupirira kuti mwina Mulungu
adzagonjetsa anthu osakhulupirira. Mulungu ndi
wamphamvu kwambiri ndi Waukali polanga. 85. Aliyense
amene amathandiza kuchita ntchito zabwino adzalandira
gawo lake la ntchitoyo, ndipo aliyense amene amathandiza
kuchita ntchito zoipa naye adzakhala ndi gawo la uchimo.
Ndipo Mulungu ali ndi mphamvu yochita chinthu china
chilichonse. 86. Ngati munthu akulonjerani onetsetsani
kuti malonje anu ndi abwino kuposa malonje ake kapena
mumubwezere monga momwe wakulonjererani. Ndithudi
Mulungu amasunga chiwerengero cha zinthu zonse.
87. Mulungu! Kulibe mulungu wina koma Iye yekha.
Ndithudi Iye adzakusonkhanitsani nonse pamodzi patsiku
louka kwa akufa, tsiku lopanda chikaiko. Kodi ndani
amalankhula zoona kuposa Mulungu?
88. Kodi mwatani kuti mukhale ogawikana magulu
awiri pa nkhani ya anthu a chinyengo? Mulungu, mwini
wake wawataya chifukwa cha ntchito zawo zoipa.
Kodi inu mufuna kumutsogolera iye amene Mulungu
wamusokeretsa? Inu simudzapeza njira ina iliyonse.
89. Iwo afuna kuti iwe usakhulupirire monga momwe iwo
sadakhulupirire kuti mulingane. Iwe usapalane nawo
ubwenzi ayi mpaka pamene asiya nyumba zawo chifukwa
cha njira ya Mulungu. Koma ngati iwo akuthawani, agwireni
ndipo muwaphe pali ponse pamene muwapeze ndipo
musafune abwenzi kapena okuthandizani pakati pawo.

90. Kupatula okhawo amene gulu lina limene liri pakati panu
ndipo inu mwachita nawo pangano lokhazikitsa mtendere
kapena adza kwa inu chifukwa mitima yawo yawaletsa
kuti amenyane nanu kapena kumenyana ndi anthu a
mtundu wawo. Mulungu akadafuna akadawapatsa iwo
mphamvu zoti akugonjetseni inu, kotero akadamenyana
nanu. Choncho ngati atalikirana nanu ndipo asiya
kumenyana nanu ndi kukuonetsani mtendere, Mulungu
wakulamulirani kuti musawaononge. 91. Mudzawapeza ena
ali kufuna chitetezo chanu ndiponso chitetezo chochokera
kwa anthu awo. Nthawi iliyonse akayesedwa iwo amapita
mwamsangamsanga. Ngati iwo sachoka kwa inu ndiponso
ngati iwo sakhazikitsa mtendere ndi inu kapena kusiya
nkhondo ndi inu, agwireni ndi kuwapha pali ponse pamene
muwapeza. Pa anthu otere, Ife takupatsani chilolezo
chomenyana nawo.

92. Ndi chinthu choletsedwa kuti munthu wokhulupirira
aphe mzake wokhulupirira kupatula mwangozi. Ndipo
aliyense amene, mwangozi, akupha munthu wokhulupirira
ayenera kumasula kapolo wokhulupirira m'modzi ndi
kulipira ndalama zopepesera ku banja la ophedwayo,
kupatula ngati iwo asankha kuti amukhululukira munthu
wakuphayo. Ngati malemuyo anali wochokera kwa
adani anu ndipo anali wokhulupirira, chilango chake ndi
kumasula kapolo m'modzi wa wokhulupirira. Koma ngati
malemuyo anali ochokera ku mtundu wa athu ogwirizana
nawo, ndalama za chipepeso ziyenera kuperekedwa
kubanja la munthu wakufayo ndi kumasula kapolo mmodzi
wa wokhulupirira. Ngati munthu sangathe kupeza izi,
ayenera kusala miyezi iwiri motsatizana ndi cholinga

chopeza chikhululukiro kwa Mulungu. Ndipo Mulungu ndi Wodziwa ndi Waluntha. 93. Ndipo aliyense amene apha munthu wokhulupirira mwadala, mphotho yake ndi kupsya ku moto wa ku Gahena ndipo adzakhala komweko ndipo mkwiyo ndi temberero la Mulungu zili pa iye ndipo chilango chowawa chili kukonzedwa chifukwa cha iye.

94. Oh inu anthu okhulupirira! Onetsetsani kuti pamene mupita kukamenya nkhondo m'njira ya Mulungu, kuti musanene kwa iwo amene akhulupirira kuti ndi osakhulupirira pofuna kuti mupeze katundu wosakhalitsa wa mdziko lino. Kwa Mulungu kuli zinthu zambiri zabwino. Monga mmene iye ali, nanunso mudali wosakhulupirira m'masiku adzana koma tsopano Mulungu wakupatsani chisomo chake pokutsogolerani ku njira yoyenera. Kotero musachite tsankho! Ndithudi Mulungu amadziwa zonse zimene mumachita. 95. Anthu okhulupirira amene akhala, safanana kupatula iwo amene ali ndi bvuto ndi amene amenyana nkhondo m'njira ya Mulungu ndi chuma chawo ndi iwo eni. Mulungu adawakweza pamwamba iwo amene amamenya nkhondo ndi chuma chawo pamodzi ndi iwo eni kuposa iwo amene akhala kunyumba. Kwa aliyense, Iye walonjeza malipiro abwino koma Mulungu wawapatsa mphotho yaikulu amene amalimbikira ndipo amamenya nkhondo m'njira ya Mulungu kuposa amene amakhala kunyumba. 96. Adzapeza maudindo kuchokera kwa Iye, chikhululukiro ndi chisoni. Mulungu amakhululukira ndipo ndi wachisoni chosatha.

97. Ndithudi! Iwo amene angelo amachotsa moyo wawo pamene ali ochimwa, adzafunsidwa kuti: "Mudali kuchita chiyani?" Iwo adzanena: "Tinali opanda mphamvu ndi

oponderezedwa padziko lapansi." Angelo adzati kwa iwo: "Kodi dziko la Mulungu silinali lotambasuka kuti inu mukadasamuka?" Iwo mudzi wawo ndi Gahena. Malo oipa kwambiri ofikirako. 98. Kupatula anthu ofoka pakati pa amuna, akazi ndi ana amene alibe mphamvu kapena njira zothawira. 99. Kwa otere pali chikhulupiriro choti Mulungu adzawakhululukira ndipo Mulungu ndi wachisoni ndi wokhululuka nthawi zonse. 100. Iye amene asamuka kwawo mu njira ya Mulungu adzapeza padziko lapansi malo ochuluka othawirako ndi katundu wochuluka. Ndipo iye amene asamuka chifukwa cha Mulungu ndi Mtumwi wake ndipo imfa impeza, ndithu malipiro ake ali ndi Mulungu. Ndipo Mulungu ndi wokhululuka ndi wachisoni chosatha.

101. Ndipo pamene inu muyenda padziko lapansi sikulakwa kwa inu kupungula mapemphero ngati muopa kuti anthu osakhulupirira akuvutitsani. Ndithudi anthu osakhulupirira ndi adani anu enieni. 102. Pamene iwe uli pakati pawo ndipo uli kuwatsogolera pa mapemphero, lola gulu lina la iwo kuti liime pamodzi ndi iwe, atanyamula zida zawo za nkhondo. Akatha kugwetsa nkhope zawo pansi apite kumbuyo kwanu ndipo libwere gulu lina limene silinapemphere kuti lipemphere nawe, ayenera kukhala tcheru ndi kutenga zida zawo za nkhondo. Anthu osakhulupirira amafuna inu mutaiwala zida zanu ndi katundu wanu kuti akukantheni nthawi imodzi, koma palibe cholakwa ngati musiya zida zanu chifukwa cha mavuto ena monga mvula kapena matenda koma khala tcheru. Ndithudi Mulungu wawakonzera anthu wosakhulupirira chilango chochititsa manyazi. 103. Pamene mumaliza mapemphero, kumbukirani Mulungu

pamene muli choimirira, chokhala pansi kapena chogona.
Koma pamene muli pabwino, pempherani nthawi zonse.
Ndithudi mapemphero ndi udindo umene udaperekedwa
kwa anthu okhulupirira kuti azichita pa nthawi zimene
zidakhazikitsidwa. 104. Ndipo musafoke pofunafuna mdani.
Ngati inu mumva kuwawa nawonso, ndithudi, akumva
kuwawa monga mmene mukuonera kuwawa inu. Koma inu
muli ndi chiyembekezo chochokera kwa Mulungu chimene
iwo alibe. Ndipo Mulungu ndi wodziwa ndi wanzeru.

105. Ndithudi Ife tavumbulutsa Buku kwa iwe
mwachoonadi kuti uweruze pakati pa anthu pogwiritsa
ntchito chimene Mulungu wakulangiza iwe. Motero
iwe usawapemphere anthu oipa. 106. Ndipo pempha
chikhululukiro cha Mulungu, ndithudi, Mulungu ndi
Wokhululukira ndi Wachisoni. 107. Ndipo iwe usawaimire
iwo amene amasokeretsa miyoyo yawo. Ndithudi Mulungu
sakonda munthu wodzipondereza yekha amene amachita
zoipa. 108. Iwo akhoza kudzibisa kwa anthu koma sangathe
kudzibisa kwa Mulungu chifukwa Iye ali pamodzi ndi
iwo pamene akonza chiwembu nthawi ya usiku ndi mawu
amene samukondweretsa. Ndipo Mulungu amadziwa
zimene iwo amachita.

109. Lo! Inu ndi amene mudawaimirira mu umoyo wa
padziko lapansi. Nanga ko di ndani amene adzawadandaulire,
kwa Mulungu pa tsiku la kuuka kwa akufa kapena ndani
amene adzakhala mtetezi wawo? 110. Ndipo iye amene
achita choipa kapena achimwira mzimu wake koma
pambuyo pake apempha chikhululukiro cha Mulungu,
adzamupeza Mulungu ali Wokhululuka ndi Wachisoni.
111. Ndipo aliyense amene achita zoipa akudzilakwira

yekha. Ndipo Mulungu ndi Waluntha ndi Wanzeru.
112. Ndipo aliyense amene achita zoipa kapena tchimo koma anamizira munthu wina wopanda chifukwa, ndithudi, iye wadzisenzetsa bodza ndi tchimo limene lili loonekera.
113. Koma pakadapanda Chisomo ndi Chisoni cha Mulungu pa iwe gulu lina la iwo likadafuna kuti likusokeretse koma iwo sangasokeretse wina aliyense koma iwo okha, ndipo iwo sangakupweteke iwe ayi. Mulungu wavumbulutsa kwa iwe Buku la luntha ndi kukuphunzitsa iwe zinthu zimene siunali kuzidziwa. Ndipo ubwino wa Mulungu pa iwe ndi waukulu zedi.

114. Mulibe zabwino zambiri muzokambirana zawo za mseri kupatula mwa iye amene amalangiza za kupereka chaulere, kuonetsa chifundo ndi chiyanjanitso pakati pa anthu, ndipo iye amene amachita izi ndi cholinga chokondweretsa Mulungu, Ife tidzampatsa mphotho yaikulu.
115. Ndipo aliyense amene amatsutsa ndi kutsutsana ndi Mtumwi, langizo lathu litaonetsedwa kwa iye ndipo atsatira njira imene siili ya anthu okhulupirira, Ife tidzamusunga mnjira imene wasankha ndipo tidzamuotcha iye ku Moto, malo onyansa kwambiri.

116. Ndithudi! Mulungu sadzakhululukira munthu wopembedza mafano. Iye adzakhululukira wina aliyense amene wamufuna pa machimo ena onse ndipo aliyense amene amalambira milungu ina osati Mulungu, iye wasochera kwambiri kuchokera ku choonadi.
117. Iwo sapembedza china koma milungu ya ikazi m'malo mwa Iye ndipo iwo sapembedza wina koma Satana wogalukira.
118. Mulungu anamutemberera iye ndipo iye adati: “Ine ndidzalanda gawo lina lokhazikika la akapolo ako.”

119. “Ndithudi ine ndidzawasocheretsa ndipo, ndithudi,
ndidzaukitsa zilakolako zawo zopanda pake ndipo,
ndithudi, ndidzawalamula kuboola makutu a ng’ombe
ndipo, ndithudi, ndidzawalamula kusintha zinthu zimene
zinalengedwa ndi Mulungu.” Ndithudi aliyense amene
asankha Satana m’malo mwa Mulungu ngati mtetezi wake,
iye ndi wotayika kodziwikiratu. 120. Iye akuwalonjeza ndi
kuwakhulupiritsa zinthu zopanda pake ndipo malonjezo
a Satana si ena koma chinyengo. 121. Malo a anthu otere
ndi Gahena ndipo sadzapeza njira yothawira kumeneko.
122. Koma iwo amene amakhulupirira ndipo amachita
ntchito zabwino, tidzawalowetsa ku Minda yothiriridwa
ndi mitsinje ya madzi yoyenda pansi pake ndipo kumeneko
adzakhalako mpaka kalekale. Lonjezo la Mulungu ndi
loona. Kodi ndani amene anganene zoona kuposa Mulungu?
123. Sikudzakhala molingana ndi zilakolako zanu kapena
za anthu a m’Buku. Iye amene achita zoipa adzalandira
zoipa, ndipo sadzapeza wina kukhala omuteteza kapena
kumuthandiza iye pambali pa Mulungu. 124. Ndipo aliyense
amene amachita ntchito zabwino, mwamuna kapena
mkazi, ndipo ndi wokhulupirira, ameneyo ndiye adzalowa
ku Paradiso ndipo sadzaponderezedwa ngakhale pang’ono.
125. Kodi ndani ali ndi chipembedzo chabwino kuposa
munthu amene amadzipereka kwathunthu kwa Mulungu
ndipo amachita ntchito zabwino ndipo amatsatira
chikhulupiriro cha Abrahamu wangwiro? Ndipo Mulungu
anamusankha Abrahamu kukhala bwenzi lake la pamtima.
126. Mwini wa chilichonse chimene chili mu mlengalenga ndi
padziko lapansi ndi Mulungu. Ndipo Mulungu amadziwa
chinthu china chilichonse.

127. Iwo amakufunsa malamulo okhudza akazi. Nena:
“Mulungu ali kukuuzani za iwo ndi zomwe zikuwerengedwa
m’buku zokhudza ana akazi a masiye amene simukuwapatsa
zimene zidalamulidwa kwa iwo komabe inu mufuna
kuwakwatira ndi ana opanda mphamvu ndi oponderezedwa
ndipo kuti muonetse chilungamo kwa ana a masiye. Ndipo
zilizonse zabwino zimene muchita, Mulungu amazidziwa.”
128. Ndipo ngati mkazi aopa kuzunzidwa kapena kusiyidwa
ndi mwamuna wake, sichidzakhala chinthu cholakwa kwa
iwo awiriwo ngati onse afuna kugwirizana pakati pawo
chifukwa mgwirizano ndi wabwino. Ndipo umunthu
umalamulidwa ndi umbombo. Koma ngati inu muchita
chinthu chabwino ndi kulewa zoipa, ndithudi Mulungu
amadziwa zonse zimene mukuchita. 129. Inu simudzatha
kuchita chilungamo pakati pa akazi anu ngakhale mutafuna
kutero. Motero musakondere mbali imodzi ndikumusiya
winayo osadziwa chimene chili kuchitika. Ndipo ngati inu
muchita chilungamo ndi kuchita chili chonse chabwino
ndi kuopa Mulungu, ndithudi Mulungu ndi wokhululukira
ndi wachisoni chosatha. 130. Koma ngati iwo asiyana,
Mulungu adzapereka zochuluka kwa aliyense wa iwo
kuchokera ku zinthu zake zambiri. Ndipo Mulungu ndi
wopereka mowolowa manja kwa zolengedwa zake ndipo
ndi Wanzeru.

131. Ndipo mwini wake wa zonse za m’mlengalenga ndi
za pa dziko lapansi ndi Mulungu. Ndipo, Ife tidawalangiza
iwo amene analandira Buku inu musadadze ndiponso ndi
inu nomwe kuti muziopa Mulungu. Koma ngati mukana,
ndithudi, Mulungu ndiye mwini wa zonse zimene zili
m’mlengalenga ndi padziko lapansi. Mulungu sasowa

chilichonse ndipo ndi Otamandidwa. 132. Ndipo mwini
wake wa zonse zimene zili mlengalenga ndi padziko lapansi
ndi Mulungu. Ndipo Mulungu ndi wokwanira kukhala
Mtetezi wanu. 133. Ngati Iye atafuna, akhoza kukuchotsani
inu ndi kubweretsa ena. Ndipo Mulungu ali ndi mphamvu
yotero. 134. Aliyense amene afuna dipo la moyo uno ndi
Mulungu yekha amene amasunga dipo la m'moyo uno ndi
umoyo umene uli nkudza. Ndipo Mulungu amamva zonse
ndipo amaona zonse.

135. Oh inu anthu okhulupirira! Khalani anthu ochita
chilungamo ngati mboni za Mulungu ngakhale kuti
umboniwo ndi wosakomera inu kapena makolo anu
kapena abale anu, kaya iwo ndi wolemera kapena wosauka.
Mulungu ndiye Mtetezi wa iwo onse. Motero musatsatire
zilakolako zanu ndi kusiya kuchita chilungamo. Ndipo
ngati mukapereka umboni wosayenera kapena kukana
kupereka, ndithudi Mulungu ali kudziwa ntchito zanu
zimene muchita.

136. Oh inu anthu okhulupirira! Khulupiririrani mwa
Mulungu ndi Mtumwi wake ndi Buku limene wavumbulutsa
kwa Mtumwi wake ndi Buku limene Iye adavumbulutsa
kale ndipo aliyense amene sakhulupirira Mulungu, Angelo
ake, Mabuku ake, Atumwi ake ndi tsiku lomaliza ndithudi
wasokera. 137. Ndithudi iwo amene akhulupirira ndipo
kenaka akana ndipo akhulupirira ndipo akananso ndipo
aonjezera kusakhulupirira, Mulungu sadzawakhululukira
kapena kuwatsogolera kunjira ya choonadi. 138. Achenjezeni
anthu achinyengo kuti chilango chowawa chili kuwadikira.
139. Iwo amene amasankha anthu osakhulupirira kukhala
atetezi awo m'malo mwa anthu okhulupirira, kodi iwo

ali kufuna ulemerero kuchokera kwa iwo? Ndithudi ulemerero, mphamvu ndi kuyamikidwa, Mwini wake ndi Mulungu.

140. Ndipo zavumbulutsidwa kale kwa inu m'Buku kuti pamene inu mukumva chivumbulutso cha Mulungu chili kukanidwa kapena kunyozedwa, inu musakhale pa malo amenewo mpaka pamene ayamba kukamba nkhani zina chifukwa mukakhala nawo, mudzakhala ngati iwo. Ndithudi Mulungu adzasonkhanitsa anthu a chinyengo ndi anthu osakhulupirira ku Gahena. 141. Iwo amene amayembekezera ndi kuyang'ana; ndipo ngati Mulungu akupambanitsani, iwo amati: "Kodi ife sitinali kumbali yanu?" Ndipo ngati anthu osakhulupirira apambana, iwo amati kwa iwo: "Kodi ife sitidali ndi mphamvu zoposa inu ndiponso kodi ife sitidakutetezeni kwa anthu okhulupirira?" Mulungu adzaweruza, pakati panu, pa tsiku lakuuka kwa akufa. Ndipo Mulungu sadzawapatsa anthu osakhulupirira njira yoti apambane anthu okhulupirira.

142. Ndithudi anthu a chinyengo afuna kunyenga Mulungu koma ndi Mulungu amene amawanyenga iwo ndipo pamene iwo amaima pamapemphero, amaimirira mwaulesi kuti anthu awaone ndipo sakumbukira Mulungu ngakhale mwapang'ono. 143. Iwo ali kupita uku ndi uko, ndipo sali m'gulu ili ndipo aliyense amene Mulungu wamusocheretsa simungampezere iye njira. 144. Oh inu anthu okhulupirira! Musasankhe anthu osakhulupirira kuti akhale abwenzi anu mmalo mwa anthu okhulupirira. Kodi mukufuna kuika umboni woonekera kwa Mulungu wokutsutsani inu? 145. Ndithudi anthu achinyengo adzaponyedwa ku malo apansipansi a ku Moto. Inu simudzawapezera

wowathandiza. 146. Kupatula iwo amene alapa zoipa zawo
ndi kuchita ntchito zabwino ndipo ayeretsa chipembedzo
chawo. Iwo adzakhala pamodzi ndi anthu okhulupirira.
Ndipo Mulungu adzawapatsa anthu okhulupirira mphotho
yaikulu. 147. Kodi Mulungu angakulangeni bwanji inu ngati
muthokoza ndi kukhulupirira mwa Iye? Ndithudi Mulungu
amayamika, ndipo ndi Wodziwa zonse.

148. Mulungu sakondwera ndi kuyankhula mawu oipa
pagulu kupatula kuchokera kwa amene waponderezedwa.
Ndipo Mulungu ndi wakumva ndi wodziwa zonse.
149. Kaya inu muonetsera pochita zabwino kapena mubisa,
kapena mukhululukira zoipa, ndithudi, Mulungu ndi
wokhululukira ndi wamphamvu zonse. 150. Ndithudi iwo
amene sakhulupirira Mulungu ndi Atumwi ake ndipo afuna
kusiyanitsa pakati pa Mulungu ndi Atumwi ake ponena
kuti: "Ife timakhulupirira mwa ena ndipo sitikhulupirira
ena." Ndipo amafuna kusankha njira yapakati ndi pakati.
151. Amenewa ndithudi ndi osakhulupirira enieni. Ndipo
Ife tawakonzera anthu osakhulupirira chilango chochititsa
manyazi. 152. Ndipo iwo amene amakhulupirira mwa
Mulungu ndi Atumwi ake ndipo sasiyanitsa pakati pa
aliyense wa iwo, Ife tidzawapatsa mphotho zawo ndipo
Mulungu ndi wokhululukira ndi wa chisoni chosatha.

153. Anthu otsatira a m'Buku akukufunsa iwe kuti
uwatsitsire buku kuchokera kumwamba. Ndithudi iwo
adafunsa Mose zazikulu kuposa zimenezi pamene iwo adati:
"Tionetse Mulungu poyera." Koma iwo anakanthidwa
ndi mphenzi chifukwa cha uchimo wawo. Ndipo iwo
adapembedza mwana wa ng'ombe ngakhale analandira
zizindikiro zathu. Komabe Ife tidawakhululukira

zimenezo. Ndipo tidampatsa Mose mphamvu zooneka. 154. Pokwaniritsa lonjezo, Ife tidakweza pamwamba pawo phiri, ndipo tidati kwa iwo: "Lowani pa chipata mogwetsa nkhope ndi modzichepetsa." Ndipo Ife tidawalamula kuti: "Musaswe malamulo a tsiku la Sabata." Ndipo Ife tidatenga lonjezo lokhazikika kuchokera kwa iwo.

155. Chifukwa chakuphwanya pangano lawo ndi kukana zizindikiro za Mulungu ndi kupha Atumwi popanda chilungamo ndi kulankhula kwawo koti: Mitima yathu ndi yokutidwa. Iyayi, Mulungu wamata mitima yawo chifukwa chakusakhulupirira kwawo. Ndipo iwo sakhulupirira kwenikweni koma pang'ono. 156. Ndi chifukwa cha kusakhulupirira kwawo ndi kulankhula zoipa za Maria, tchimo lalikulu. 157. Ndikulankhula kwawo koti: "Ife tidamupha Messiya, Yesu mwana wamwamuna wa Maria, Mthenga wa Mulungu," koma iwo sadamuphe ayi ndipo sadampachike koma maonekedwe a Yesu anaikidwa pa munthu wina ndipo iwo amene amatsutsa za izo ndi okaika. Iwo sadziwa chili chonse, koma akutsatira nkhani za m'maluwa. Ndithudi iwo sadamuphe ayi. 158. Koma Mulungu adamukweza kudza kwa Iye. Ndipo Mulungu ndi wa mphamvu ndi Wanzeru.

159. Ndipo palibe mmodzi wa anthu a m'Buku amene angakhulupirire mwa iye, asadafe. Ndipo patsiku louka kwa akufa, iye adzakhala mboni yowatsutsa iwo. 160. Chifukwa chakulakwa kwa Ayuda, Ife tidawaletsa chakudya china chabwino chimene chidali chololedwa kwa iwo ndi chifukwa chotsekereza anthu ambiri mnjira ya Mulungu. 161. Ndi kulandira kwawo kwa katapira pamene iwo ataletsedwa kutero, ndi kudya kwawo kwa chuma

cha anthu mwachinyengo. Ndipo Ife takonza chilango chowawa cha anthu osakhulupirira amene ali pakati pawo. [162.] Koma iwo ozindikira kwambiri amene ali pakati pawo ndi okhulupirira amene amakhulupirira mu zimene zavumbulutsidwa kwa iwe ndi zimene zidavumbulitsidwa iwe usanadze, ndipo amapemphera nthawi zonse ndikupereka msonkho wothandiza anthu osauka ndipo ali ndi chikhulupiriro mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza, awa ndiwo amene Ife tidzawapatsa mphotho yaikulu.

[163.] Ife tavumbulutsa kwa iwe monga momwe tidavumbulutsira kwa Nowa ndi kwa Atumwi ena amene anadza pambuyo pa iye. Ndipo tidavumbulutsa kwa Abrahamu, Ishimayeli, Isake, Yakobo ndi a mitundu, Yesu, Yobu, Yona, Aroni ndi Solomoni ndipo Davide tidamupatsa Buku la Masalimo. [164.] Ndi Atumwi amene Ife takuuza kale mbiri yawo ndi Atumwi amene sitidakuuze ayi, ndipo ndi Mose Mulungu adalankhula naye mwachindunji. [165.] Atumwi ngati obweretsa nkhani zabwino kwa mitundu ya anthu ndipo chenjezo kuti iwo asadzakhale ndi chodandaula kwa Mulungu pambuyo pa Atumwi. Ndipo Mulungu ndi Wamphamvu nd Wanzeru.

[166.] Koma Mulungu achitira umboni pa zimene wavumbulutsa kwa iwe, Iye walitumiza ndi nzeru zake ndipo angelo achitira umboni. Ndipo Mulungu ndi wokwana kukhala mboni. [167.] Ndithudi iwo amene sakhulupirira ndipo amaletsa ena kutsatira njira ya Mulungu, ndithudi, asochera kwenikweni. [168.] Ndithudi iwo amene sakhulupirira ndipo adachita zosalungama, Mulungu sazawakhululukira ndipo sadzawatsogolera kunjira ina. [169.] Kupatula njira ya ku Gahena, kuti adzakhaleko mpaka kalekale. Ndipo

imeneyi ndi ntchito yopepuka kwa Mulungu. 170. Oh inu
anthu! Ndithudi wadza kwa inu Mtumwi ndi choonadi
chochokera kwa Ambuye wanu, motero khulupirirani
mwa iye ndipo zonse zidzakhala bwino kwa inu. Ngati inu
simukhulupirira ndithudi mwini wa chilichonse chimene
chili mlengalenga ndi padziko lapansi ndi Mulungu. Ndipo
Mulungu ndi wodziwa chilichonse ndi Wanzeru.
171. Oh inu anthu a m'Buku! Musadutse malire a
chipembedzo chanu kapena kunena zokhudza Mulungu
kupatula choonadi. Messiya Yesu, mwana wa Maria, sadali
wina aliyense koma Mtumwi wa Mulungu ndi Mawu ake
amene adanena kwa Maria, ndi Mzimu wolengedwa ndi
Iye. Kotero khulupirirani mwa Mulungu ndi Atumwi
ake. Ndipo musanene kuti: "Atatu." Siyani! Zidzakhala
bwino kwa inu. Chifukwa Mulungu ndi mmodzi yekha.
Ulemerero ukhale kwa Iye. Iye sangakhale ndi mwana.
Zake ndi zonse zimene zili kumwamba ndi pa dziko lapansi.
Ndipo Mulungu ndi okwana kukhala Mtetezi wodalirika.
172. Messiya sangakane kukhala kapolo wa Mulungu
ndiponso angelo amene ali kufupi ndi Mulungu. Ndipo
aliyense amene amakana kumutumikira Mulungu chifukwa
cha kudzikweza, Iye adzawasonkhanitsa onse kudza
pamaso pake. 173. Motero iwo amene ali ndi chikhulupiriro
ndipo amachita ntchito zabwino, Iye adzawapatsa
mphotho zawo mokwanira ndipo adzawalemeretsa iwo
mwachisomo chake chochuluka. Koma iwo amene akana
kupembedza kapena oyerekedwa, Iye adzawalanga ndi
chilango chowawa. Ndipo iwo sadzapeza wina woposa
Mulungu kuti awateteze kapena kuwathandiza. 174. Oh
inu anthu! Ndithudi wadza kwa inu umboni wooneka

kuchokera kwa Ambuye wanu ndipo Ife takutumizirani Muuni woonekera. 175. Motero iwo amene amakhulupirira mwa Mulungu ndipo amadzipereka kwathunthu kwa Iye, adzawalowetsa ku chifundo ndi chisomo chake ndi kuwatsogolera kunjira yoyenera. 176. Iwo amakufunsa za malamulo; Nena: “Mulungu akukuuzani za munthu amene alibe makolo kapena mwana. Ngati munthu wa mwamuna akufa, ndipo alibe mwana koma ali ndi mlongo wake, mlongo wake adzalandire theka la katundu amene asiya. Ndipo ngati mkazi sasiya mwana, mlongo wake adzatenga chuma chake. Koma ngati akhala ndi alongo ake awiri, iwo adzalandire magawo awiri a magawo atatu a katundu amene asiya. Ndipo ngati pali abale amuna ndi akazi, mwamuna adzalandira magawo amene angalandire akazi awiri. Mulungu akukulongosolerani kuti musasochere. Ndipo Mulungu ndi wodziwa chilichonse.”

Sura 5 • Al-Mâ-idah

# Al Maidah

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Oh inu anthu okhulupirira! Kwaniritsani mapangano anu. Ndi zololedwa kwa inu kudya nyama zonse kupatula zimene tsopano zili kuletsedwa kwa inu. Kusaka nyama ndi koletsedwa pamene muli paulendo wa Hajji. Ndithudi Mulungu amalamula zimene Iye afuna. 2. Oh inu anthu okhulupirira! Musaphwanye kupatulika kwa zizindikiro za

Mulungu kapena za Mwezi Woyera kapena za nyama zimene zimabweretsedwa kukhala nsembe kapena zizindikiro zimene zimaikidwa pa izo kapena za anthu amene amadza ku Nyumba Yoyera kudzafuna chisomo ndi chisangalalo cha Ambuye wawo. Koma mukatsiriza miyambo ya Hajji, mukhoza kusaka ndipo musalole chidani cha anthu ena amene anakuletsani kulowa mu Mzikiti Woyera kuti chikuchimwitseni. Thandizanani wina ndi mnzake pa ntchito zabwino koma musathandizane mu ntchito ya uchimo ndi yoswa malamulo. Muopeni Mulungu. Ndithudi Mulungu amalanga kwambiri.

3. Zoletsedwa kwa inu kudya ndi nyama yofa yokha, liwende, nyama ya nkhumba ndi nyama iliyonse imene yaphedwa m'dzina la mulungu wina osati Mulungu weniweni. Inu muli kuletsedwa kudya nyama zophedwa pomangirira chingwe pakhosi ndi kukoka ndiponso izo zimene zamenyedwa mpaka kufa, nyama zimene zaphedwa chifukwa chakugwa kapena yaphedwa ndi nyama inzake ndiponso imene yadyedwa ndi chilombo cha m'thengo, kupatula ngati inu mwaimaliza kupha ndiponso nyama zimene zaphedwa pamwala ndi kuperekedwa ku milungu ya mafano. Inu mwaletsedwa kufuna kudziwa chinsinsi pochita mayere a maula. Amenewa ndi machitidwe oipa . Lero anthu osakhulupirira achita mantha ndi chipembedzo chanu. Motero musawaope iwo koma opani Ine. Lero ndakonza chipembedzo chanu ndipo ndamaliza ubwino wanga pa inu ndipo Ine ndakusankhirani Chisilamu kuti chikhale chipembedzo chanu. Koma iye amene wakakamizidwa ndi njala osati ndi cholinga chochimwa, ndithudi, Mulungu ali wokhululukira ndi wachisoni.

4. Iwo amakufunsa iwe za zinthu zimene zili zololedwa
kwa iwo. Nena: “Zinthu zonse zimene ndi zabwino ndi
zololedwa kwa inu ndiponso zinthu zimene mwaphunzitsa,
mbalame ndi nyama zosaka kuti zizigwira, kuziphunzitsa
monga momwe Mulungu adakuphunzitsirani. Motero
idyani zimene izo zakugwirirani koma tchulani dzina la
Mulungu pa izo ndipo opani Mulungu. Ndithudi Mulungu
ndi wachangu powerengera.” 5. Zinthu zonse zabwino,
tsiku lalero, zaloledwa kuti mukhoza kuzigwiritsa ntchito.
Chakudya cha anthu m’Buku ndi chololedwa kwa inu
ndiponso chakudya chanu ndi chololedwa kwa iwo.
Muloledwa kukwatira akazi okhulupirira ndi akazi angwiro
kuchokera ku gulu la anthu a m’Buku pamene muwapatsa
mphatso yawo ya ukwati ndi kukhala molemekezeka ndi
iwo osachita chiwerewere kapena kuwasandutsa iwo ngati
zibwenzi zanu. Ndipo aliyense amene sakhulupirira mwa
Mulungu mmodzi, ntchito zake zidzakhala zopanda pake
ndipo m’dziko limene lili nkudza, iye adzakhala olephera
kwambiri.

6. Oh inu anthu okhulupirira! Pamene mukonzeka kuti
mupemphere, sambitsani nkhope zanu ndiponso manja
anu mpaka pa kasukusuku ndipo pakani ku mutu kwanu
ndipo sambitsani mapazi anu mpaka molekezera phazi
lanu. Ngati mwadetsedwa, dziyeretseni. Koma ngati muli
kudwala kapena muli paulendo, kapena wina wa inu abwera
kuchokera ku chimbudzi kapena munagona ndi akazi
anu ndipo mwasowa madzi, tengani mchenga woyera ndi
kupukuta m’manja mwanu ndi ku nkhope kwanu. Mulungu
safuna kukukundikirani mtolo wolemera koma Iye afuna

kukuyeretsani ndi kukwaniritsa zokoma zake kwa inu kuti
inu mukhale oyamika.

7. Ndipo kumbukirani zabwino zimene Mulungu
wakupatsani inu ndi lonjezo limene adakumangani nalo
pamene inu mudanena kuti: "Tamva ndipo tidzatsatira."
Ndipo muopeni Mulungu. Ndithudi Iye amadziwa
maganizo amene ali mu mtima mwanu. 8. Oh inu anthu
okhulupirira! Limbikirani chifukwa cha Mulungu
ndipo perekani umboni woona wokhawokha ndipo
musalole chidani chimene chilipo ndi anthu ena kuti
chikusokonezeni kuchita chilungamo. Chitani chilungamo
chifukwa chilungamo chili kufupi ndi kuyera mtima ndipo
opani Mulungu. Ndithudi Mulungu amadziwa ntchito
zonse zimene mumachita. 9. Mulungu walonjeza onse amene
amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino, kuti
kwa iwo kuli chikhululukiro ndiponso mphotho yaikulu.
10. Iwo amene sakhulupirira ndipo amakana chivumbulutso
chathu, amenewa adzakhala eni ake a Gahena. 11. Oh inu
anthu okhulupirira! Kumbukirani ubwino wa Mulungu pa
inu pamene anthu ena adafuna kukutambasulirani manja
awo koma Mulungu adatchinjiriza manja awo kufika kwa
inu. Motero opani Mulungu. Ndipo mwa Mulungu, alekeni
anthu okhulupilira kuti aike chikhulupiriro chawo.

12. Ndithudi Mulungu adalandira lonjezo la ana a Israyeli
ndipo Ife tidadzutsa pakati pawo atsogoleri khumi ndi
awiri. Ndipo Mulungu adati: "Ine, ndithudi, ndili pamodzi
ndi inu ngati inu mupemphera moyenera, mupereka
chopereka chothandiza anthu osauka ndipo mukhulupirira
mwa Atumwi anga ndipo muwathandiza ndiponso
mukongoza Mulungu ngongole yabwino. Ndithudi Ine

ndidzakukhululukirani machimo anu ndi kukulowetsani ku minda yothiririridwa ndi madzi ya m'mitsinje. Koma ngati wina wa inu, pambuyo pake sakhulupilira, Iye wasochera ku njira yoyenera." [13.] Koma chifukwa chakuti iwo adaphwanya lonjezo lawo, Ife tidawatemberera ndi kuumitsa mitima yawo. Iwo adasintha mawu ndi kuwachotsa m'malo mwake ndi kusiya zambiri zimene zidatumizidwa kwa iwo. Siudzasiya kuona ntchito za chinyengo mwa iwo kupatula owerengeka okha. Koma akhululukire ndipo uwalekerere. Ndithudi Mulungu amakonda anthu ochita zabwino.

[14.] Ndipo kuchokera kwa iwo amene amadzitcha kuti ndi Akhirisitu. Ife tidachita nawo lonjezo koma iwo adasiya zambiri zimene zidatumizidwa kwa iwo. Kotero tidadzutsa pakati pawo udani ndi chizondi chimene chidzakhala mpaka patsiku louka kwa akufa ndipo Mulungu adzawauza iwo zonse zimene amachita.

[15.] Oh inu anthu a m'Buku! Ndithudi Mtumwi wathu wadza kudzakuuzani inu zambiri zimene mwakhala mukuzibisa za m'Buku la Mulungu ndi kuzisiya osafotokoza bwino. Ndithudi kwadza kuwala kwa inu kuchokera kwa Mulungu ndi Buku la choonadi. [16.] Limene Mulungu amatsogolera, kunjira ya mtendere, onse amene amafuna chikondwerero cha Iye. Mulungu amawatulutsa, mwachifuniro chake, kuchoka ku mdima ndi kunka kowala, ndipo amawatsogolera kunjira yoyenera. [17.] Ndithudi ndi chifukwa chopanda chikhulupiliro chimene iwo amati: "Mulungu ndi Messiya, mwana wa Maria." Nena: "Kodi ndani amene angamuletse Mulungu ngati Iye atafuna kuononga Messiya mwana wa Maria, Mai wake ndi zonse zimene zili m'dziko lapansi?" Mwini ufumu wakumwamba

ndi dziko lapansi ndi zonse zimene zili m'menemo ndi
Mulungu. Iye amalenga chimene afuna. Ndipo Iye ali ndi
mphamvu pa chinthu chilichonse.
18. Ndipo Ayuda ndi Akhirisitu amati: "Ife ndife ana
a Mulungu ndiponso wokondedwa ake." Nena: "Nanga
bwanji amakulangani chifukwa cha zolakwa zanu?" Iyayi,
inu ndinu anthu amene mudalengedwa ndi Iye. Mulungu
amakhululukira aliyense amene Iye wamufuna ndipo
amalanga aliyense amene Iye wamufuna. Mwini ufumu wa
kumwamba ndi dziko lapansi ndi zonse zili m'menemo ndi
Mulungu. Ndipo kwa Iye ndiko kobwerera. 19. Oh inu anthu
otsatira Buku! Tsopano mtumwi wathu wadza kwa inu
kudzaulula poyera chifuniro chathu patapita nthawi yaitali
imene kudalibe Atumwi, kuti mwina mungadzanene kuti:
"Sikudabwere kwa ife wodzatiuza nkhani zabwino kapena
kudzatichenjeza." Ndipo Mulungu ali ndi mphamvu pa
chinthu china chilichonse.
20. Ndi pamene Mose adawauza anthu ake: "Oh
Anthu anga! Kumbukirani zokoma zimene Mulungu
wakuchitirani inu pamene adaika Atumwi pakati panu,
adakupangani inu kukhala mafumu ndipo adakupatsani
zimene sadampatsepo wina aliyense mu zolengedwa
zonse." 21. Oh anthu anga! Lowani m'dziko loyera limene
Mulungu wakupatsani ndipo musabwerere m'mbuyo
chifukwa mudzabwezedwa ngati olephera pa zochita.
22. Iwo adati: "Iwe Mose! Kumeneko kuli anthu amphamvu
ndipo ife sitidzalowa m'dziko limeneli pokhapokha iwo
atachoka ndipo ngati iwo atatuluka, ife tidzalowamo."
23. Anthu awiri amene amaopa ndiponso amene Mulungu
adaonetsa chisomo chake adati: "Amenyeni kudzera pa

chipata, chifukwa ngati inu mulowa, mudzapambana ndipo
ikani chikhulupiliro chanu mwa Mulungu ngati inu ndinu
wokhulupilira.” 24. Iwo adati: “Iwe Mose! Ife sitidzalowa
m’menemo ngati iwo akhalabe ali momwemo. Motero pita
iwe pamodzi ndi Ambuye wako, kukamenyana nawo. Ife
tikhala pompano.”
25. Iye adati: “Ambuye wanga! Ine ndili ndi mphamvu pa
ine mwini ndi pa mbale wanga, motero tipatuleni kugulu
la anthu oswa malamulo.” 26. Mulungu adati: “Motero iwo
sadzalowa m’dziko ili mpaka patatha zaka makumi anayi
ndipo adzakhala akuyendayenda wopanda malo enieni
padziko lapansi. Motero usawadandaulire anthu oswa
malamulo.”
27. Ndipo auze iwo, mwachoonadi, nkhani za ana awiri
a Adamu mmene aliyense adaperekera nsembe yake ndi
kulandiridwa kwa nsembe ya mmodzi wa iwo pamene ya
wina siidalandiridwe. Iye adati: “Ndithudi ine ndikupha.”
Ndipo m’bale wake adati: “Mulungu amalandira nsembe ya
anthu olungama.” 28. “Ngati iwe utambasula dzanja lako kuti
undiphe, ine sindidzatambasula dzanja langa kuti ndikuphe
chifukwa ine ndimaopa Mulungu, Ambuye wazolengedwa
zonse.” 29. “Ndithudi ine ndikufuna kuti usenze machimo
anga ndi ako ndipo udzakhala m’gulu la anthu a ku Moto
ndipo imeneyi ndi mphotho ya anthu ochita zoipa.”
30. Motero mtima wake udamuumiriza kupha m’bale
wake! Iye adamupha ndipo adakhala mmodzi wa
anthu olephera. 31. Ndipo atatero Mulungu adatumiza
khwangwala amene adakumba pansi ndi kumulangiza
mmene iye angakwiririre mtembo wa m’bale wake. Iye
adati: “Kalanga ine! Ndalephera kukhala ngati khwangwala

uyu ndi kukwirira mtembo wa m'bale wanga?" Ndipo iye
adali mmodzi wa anthu onong'oneza bombono.
32. Chifukwa cha chimenechi Ife tidakhazikitsa lamulo
kwa ana a Israyeli kuti ngati wina apha munthu mnzake
osati chobwezera imfa ya wina kapena kuyambitsa
chisokonezo pa dziko adzakhala ngati wapha anthu
onse, ndipo kuti ngati wina adzapulumutsa moyo wa
munthu, adzakhala ngati kuti adapulumutsa anthu onse.
Ndithudi adabwera kwa iwo Atumwi athu ndi zizindikiro
zooneka komabe sipanapite nthawi mmene ena a iwo
adachimwa machimo akuluakulu m'dziko. 33. Mphotho ya
iwo amene amamenya nkhondo yolimbana ndi Mulungu
ndi Mtumwi wake ndipo amafalitsa chisokonezo m'dziko
ndi kuphedwa kapena kupachikidwa pa mtanda kapena
kudulidwa manja ndi mapazi awo mosiyanitsa mbali
kapena kuthamangitsidwa m'dziko. Zimenezo, kwa iwo,
ndi zowachititsa manyazi m'dziko lino ndipo adzalangidwa
kwambiri m'dziko limene lili kudza. 34. Kupatula okhawo
amene alapa iwe usadawagonjetse. Motero dziwani kuti
Mulungu ndi wokhululukira ndi wachisoni chosatha.
35. Oh inu anthu okhulupirira! Opani Mulungu ndipo
funani njira yoyenera yopita kwa Iye ndipo limbikirani
kwambiri m'njira ya Mulungu kuti mukhale opambana.
36. Ndithudi anthu osakhulupirira, akadakhala nazo
zonse zimene zili padziko ndi zina zoonjezera apa kuti
adzipulumutsire nazo ku chilango cha patsiku louka
kwa akufa, sizidzalandiridwa kuchokera kwa iwo ndipo
chawo chidzakhala chilango chowawa. 37. Iwo adzayesetsa
kuti achoke kumoto koma sadzatha kuchoka ayi ndipo
chawo chidzakhala chilango chosatha. 38. Kwa munthu

wakuba, mwamuna kapena mkazi, m'duleni dzanja lake
ngati malipiro a zimene wachita ndi chilango ngati
chitsanzo chochokera kwa Mulungu. Ndipo Mulungu ndi
mphamvu ndi waluntha. 39. Koma aliyense amene alapa
pambuyo pochimwa, ndipo achita ntchito zabwino, ndithu
Mulungu adzalandira kulapa kwake. Ndithudi Mulungu
ndi Okhululukira ndi Wachisoni chosatha. 40. Kodi iwe
siudziwa kuti Mulungu ndiye Mwini ufumu wa kumwamba
ndipo dziko lapansi? Iye amalanga amene wamufuna
ndipo amakhululukira aliyense amene wamufuna. Ndipo
Mulungu ndi wamphamvu pa chinthu china chilichonse.
41. Oh iwe Mtumwi! Asakudandaulitse anthu amene
amafulumira kusakhulupirira ndipo amati: "Tikhulupirira"
ndi milomo yawo pamene mitima yawo ilibe chikhulupiriro.
Ndipo pakati pa Ayuda pali anthu amene amamvetsera
mabodza ndi zimene anthu ena amene sadadze kwa iwe
amakamba. Iwo amasintha mawu monga momwe adalili
ndipo amati: "Ngati mwapatsidwa izi landirani ndipo
ngati simudapatsidwe chenjerani." Ndipo amene Mulungu
afuna kumusocheretsa,iwe ulibe mphamvu ina iliyonse pa
iye yopikisana ndi Mulungu. Awo ndi amene mitima yawo
Mulungu safuna kuiyeretsa ndipo kwa awa kuli zinthu
zochititsa manyazi m'dziko lino ndi chilango chachikulu
m'dziko limene lili nkudza.
42. Iwo amakonda kumvera nkhani zabodza ndi kumadya
zinthu zoletsedwa. Ndipo ngati iwo adza kwa iwe, uweruze
pakati pawo kapena ungowasiya. Ngati iwe uwasiya,
iwo sangathe kukupweteka ayi, koma ngati uwaweruza,
weruza mwachilungamo pakati pawo. Ndithudi Mulungu
amakonda iwo amene amachita chilungamo. 43. Kodi iwo

abwera bwanji kwa iwe kudzaweruzidwa pamene iwo ali
ndi Buku la chipangano chakale limene muli chiweruzo cha
Mulungu? Ndipo ngakhale zili tero iwo amatembenuka.
Iwo si okhulupirira enieni. 44. Ndithudi Ife tidavumbulutsa
chipangano chakale mmene muli chilangizo ndiponso
kuwala, ndipo kudzera mu ilo, Atumwi amene anadzipereka
kwa Mulungu, adaweruza Ayuda. Ndipo Ansembe ndi
anthu oyera mtima chifukwa iwo adapatsidwa udindo
osamala Buku la Mulungu, ndipo iwo adali mboni. Motero
usamaope anthu koma opani Ine ndipo musasinthitse
chivumbulutso changa ndi zinthu zopanda pake. Ndipo
yense amene salamulira ndi zomwe adatumiza Mulungu,
iwo ndi anthu osakhulupirira. 45. Ndipo mu ilo, Ife
tidalamula kuti moyo ku moyo, diso ku diso, mphuno ku
mphuno, khutu ku khutu, dzino ku dzino ndi ululu ku ululu.
Koma ngati munthu akhululuka chifukwa chowonetsa
chisoni, chimenechi chidzakhala chikhululukiro. Ndipo
aliyense amene saweruza ndi zomwe adavumbulutsa
Mulungu, woteroyo ndi opanda chilungamo. 46. Atapita
awa, Ife tidatumiza Yesu, mwana wamwamuna wa Maria
kudzatsimikiza za Buku la chipangano chakale limene
lidavumbulitsidwa kale ndipo tidamupatsa Iye chipangano
chatsopano m'mene muli ulangizi ndi muuni wotsimikiza
zonse zimene zidavumbulutsidwa kale m'buku la
chipangano chakale, ulangizi ndi chenjezo kwa anthu
oyera mtima. 47. Anthu a m'Buku la chipangano chatsopano
aweruze potsatira zimene Mulungu wavumbulutsa
m'menemo. Ndipo aliyense amene saweruza molingana
ndi chivumbulutso cha Mulungu ndi olakwa.

48. Ndipo kwa iwe, tavumbulutsa Buku mwachoonadi

kutsimikiza Mabuku amene adadza kale, okhulupilika
ndi a pamwamba. Kotero weruza pakati pawo ndi zimene
wavumbulutsa Mulungu ndipo usatsatire zilakolako zawo
kusiya choonadi chimene chavumbulutsidwa kwa iwe. Ife
takhazikitsa lamulo ndipo takonza njira yoyenera. Ngati
Mulungu akadafuna, akadakupangani inu kukhala mtundu
umodzi wa anthu koma afuna kuti akuyeseni inu ndi zimene
wakupatsani. Motero pikisanani pochita ntchito zabwino.
Ndi kwa Mulungu kumene nonsenu mudzabwerera ndipo
Iye adzakuuzani zonse zimene munali kutsutsana.
49. Ndipo motero weruza pakati pawo molingana ndi
chivumbulutso cha Mulungu ndipo usatsatire zilakolako
zawo, ndipo chenjera nawo chifukwa akhoza kukubweza
kugawo limene Mulungu wavumbulutsa kwa iwe. Koma
ngati iwo akana chiweruzo chako, dziwani kuti chifuniro
cha Mulungu ndi kuwalanga chifukwa cha zoipa zawo.
Ndithudi anthu ambiri ndi oswa malamulo. 50. Kodi ndi
malamulo a chikunja amene iwo afuna kuti aweruzidwe
nawo? Kodi woweruza wabwino kwambiri ndani woposa
Mulungu kwa anthu amene ali ndi chikhulupiriro cholimba?
51. Oh inu anthu okhulupirira! Musasankhe Ayuda ndi
Akhirisitu kuti akhale abwenzi anu. Iwo ndi abwenzi a
wina ndi mnzake ndipo aliyense wa inu amene apalana
nawo chibwenzi ndithudi adzakhala mmodzi wa iwo.
Ndithudi Mulungu satsogolera anthu ochita zoipa.
52. Ndipo iwe umawaona anthu amene ali ndi matenda
m'mitima mwawo ali kuwathamangira abwenzi awo nati:
"Tili kuopa kuti mwina tsoka likhoza kutigwera ife."
Mwina Mulungu akhoza kubweretsa kupambana kapena
lamulo mwachifuniro chake. Ndipo iwo adzadandaula

chifukwa cha zimene adasunga ngati chinsinsi mwa iwo
okha. 53. Ndipo anthu okhulupirira adzati; “Kodi awa ndi
anthu omwe analumbira molimbika kuti, pali Mulungu,
iwo ali pamodzi ndi inu?” Ntchito zawo zonse zidzakhala
zopanda pake ndipo iwo akhala olephera.
54. Inu anthu okhulupirira! Aliyense wa inu amene asiya
chipembedzo chake, Mulungu adzaika anthu wolowa
m’malo mwake ndipo Mulungu adzawakonda anthuwo
ndiponso anthuwo adzakonda Mulungu, odzichepetsa
kwa anthu okhulupirira koma olimba kwa anthu
osakhulupirira, omenya nkhondo munjira ya Mulungu
ndipo osaopa zonena za anthu. Chimenechi ndicho
chisomo cha Mulungu chimene Iye amachipereka kwa
aliyense amene Iye wamufuna. Ndipo Mulungu ali ndi
zonse zimene zolengedwa zake zimafuna, Iye amadziwa.
55. Ndithudi bwenzi lanu lapamtima ndi Mulungu, Mtumwi
wake ndi anthu okhulupirira amene amapemphera nthawi
zonse ndipo amapereka zopereka ndipo amadzichepetsa
akamapembedza. 56. Ndipo amene amasankha Mulungu,
Mtumwi wake ndi anthu onse okhulupirira kukhala
omuteteza ayenera kudziwa kuti gulu la Mulungu
lidzapambana.
57. Oh inu okhulupirira! Musapalane chibwenzi ndi
anthu amene amachita chipongwe chipembedzo chanu
ndi kuchisandutsa kukhala choseweretsa, amene ali
pakati pa anthu amene adapatsidwa mau a Mulungu kale
inu musanadze kapena anthu osakhulupirira ndipo opani
Mulungu ngati inu ndinu anthu okhulupirira. 58. Ndipo
ngati inu muitanira mapemphero, iwo amaganiza kuti ndi
nthabwala ndiponso chinthu choseweretsa chifukwa iwo

ndi anthu opanda nzeru. 59. Nena: “Oh inu anthu a m’Buku!
Kodi inu muli kutitsutsa ife chifukwa chakuti takhulupirira
mwa Mulungu ndi mwa zimene zavumbulutsidwa kwa
ife ndiponso zimene zidavumbulutsidwa kale ndipo kuti
ambiri a inu ndinu anthu ochita zoipa?” 60. Nena: “Kodi ine
ndikuuzeni chinthu chonyasa kuposa ichi chochokera kwa
Mulungu? Iwo amene Mulungu adawatemberera ndipo
adawakwiyira ndikuwasintha kukhala nyani ndi nkhumba,
iwo amene amapembedza milungu yabodza. Awa ndi anthu
apansi zedi ndipo ndi osochera kunjira yoyenera.”
61. Ndi pamene iwo amadza kwa inu amati: “Ife
takhulupirira.” Koma iwo amalowa ali osakhulupirira
ndipo amatuluka ndi kusakhulupirira. Ndipo Mulungu
amadziwa zonse zimene amabisa. 62. Ndipo iwe umawaona
ambiri a iwo ali kupikisana m’machimo ndi mu zinthu
zodanitsa ndipo ali kudya zinthu zosaloledwa. Ndithudi
ndi zoipa zimene iwo akhala ali kuchita. 63. Kodi ndi
chifukwa chiyani Abusa ndiponso anthu Oyera, sawaletsa
anthu kulankhula mawu amachimo kapena kudya zinthu
zoletsedwa? Ndithudi zoipa ndi zimene iwo akhala ali
kuchita.
64. Ayuda amanena kuti: “Manja a Mulungu ndi omangika.”
Manja awo ndiwo akhale omangika ndiponso iwo
atembereredwe chifukwa cha zimene anena! Iyayi! Manja
onse a Mulungu ndi otambasuka. Iye amapereka mmene
wafunira. Ndithudi chimene Mulungu wavumbulutsa kwa
iwe chimaonjezera udani ndi kusakhulupirira kwa anthu
ambiri mwaiwo. Ife taika pakati pawo ndi kukhazikitsa
udani mpaka patsiku louka kwa akufa. Nthawi zonse
pamene iwo ayatsa moto wa nkhondo, Mulungu amauzima

ndipo iwo amayesetsa kupanga zoipa padziko. Mulungu sakonda anthu oyambitsa chisokonezo.

65. Akadakhala kuti anthu a m'Buku adakhulupirira ndi kulewa zoipa, Ife tikadawakhululukira machimo awo ndi kuwalowetsa m'minda ya mtendere.
66. Ndipo iwo akadatsatira Buku la chipangano chakale ndi chipangano chatsopano ndiponso zimene zavumbulutsidwa kwa iwo kuchokera kwa Ambuye wawo, iwo akadadya zinthu kuchokera kumwamba ndi pansi pa miyendo yawo. Ena mwa iwo ndi anthu a chilungamo koma ambiri a iwo ndi ochita zoipa.

67. Oh iwe Mtumwi! Lalikira zimene zavumbulutsidwa kwa iwe kuchokera kwa Ambuye wako. Ndipo ngati iwe siutero, ndithudi, iwe walephera kupereka uthenga wake. Mulungu adzakuteteza iwe kwa anthu. Ndithudi Mulungu satsogolera anthu osakhulupirira.

68. Nena: "Oh inu anthu a m'Buku! Inu mulibe poimira mpaka pamene mutatsatira Buku la chipangano chakale ndi chipangano chatsopano ndi zimene zavumbulutsidwa kwa inu kuchokera kwa Ambuye wanu." Ndithudi zimene zavumbulutsidwa kwa iwe kuchokera kwa Ambuye wako ziwonjezera, mwa ambiri a iwo, machimo ndi kusakhulupirira. Motero iwe usamve chisoni ndi anthu osakhulupirira.
69. Ndithudi iwo amene amakhulupirira ndi iwo amene ndi Ayuda, Masabiyani ndi Akhirisitu, aliyense amene amakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku la chimaliziro ndipo amachita zabwino, iwo sadzakhala ndi mantha ndipo sadzadandaula.
70. Ndithudi Ife tidalandira lonjezo kuchokera kwa ana a Israyeli ndipo tidatumiza Atumwi kwa iwo. Koma nthawi iliyonse imene Mtumwi

amadza kwa iwo ndi uthenga umene mitima yawo
siimafuna, iwo adali kunena kuti ena ndi onama pamene
ena adali kuwapha. 71. Iwo adali kuganiza kuti padalibe
chilango chimene chikadawatsata, motero iwo adakhala a
khungu ndi osamva. Ndipo Mulungu adawakhululukira iwo
komabe ambiri a iwo adali a khungu ndi osamva. Mulungu
amaona zonse zimene akuchita.
72. Ndithudi ndi osakhulupirira amene amati: "Mulungu
ndi Messiya mwana wa mwamuna wa Maria." Koma
Messiya mwini wake adati: "O inu ana a Israyeli!
Pembedzani Mulungu, Ambuye wanga amene ndi Ambuye
wanu."Ndithudi aliyense amene apembedza milungu
ina m'malo mwa Mulungu yekha sadzalowa ku Paradiso
ndipo malo ake ndi kumoto. Ndipo anthu ochita zoipa
alibe owathandiza. 73. Ndithudi osakhulupirira ndi anthu
amene amati: "Mulungu ndi mmodzi mwa atatu." Koma
kulibe Mulungu wina koma mmodzi yekha. Ndipo ngati
iwo sasiya zimene akunena, ndithudi chilango chowawa
chidzagwa pa anthu osakhulupilira amene ali pakati
pawo. 74. Kodi iwo sangalape kwa Mulungu ndi kufunsa
chikhululukiro chake? Mulungu ndi wokhululukira ndi
wachisoni chosatha. 75. Messiya, mwana wamwamuna
wa Maria, sadali wina aliyense ayi koma Mtumwi,
Atumwi ena adadza iye asadadze. Mayi wake adali mayi
wokhulupilira. Onse adali kudya chakudya. Taona mmene
timaonetsera kwa iwo poyera chivumbulutso chathu ndipo
taona mmene iwo amatembenuzira choonadi. 76. Nena:
"Kodi inu muzipembedza, powonjezera pa Mulungu,
chinthu chimene sichingathe kukuonongani kapena

kukuthandizani?" Koma Mulungu ndiye amamva zonse
ndiponso amadziwa zonse.
77. Nena: "Inu anthu a m'Buku! Musaonjezere china
chilichonse m'chipembedzo chanu chosakhala choonadi
ndipo musatsatire zilakolako za anthu amene adasokera
kale, amene anasocheretsa anthu ochuluka ndiponso
adadzisocheretsa iwo eni kunjira yoyenera."
78. Iwo amene adali pakati pa ana a Israyeli, ndipo
sanakhulupilire, anatembereredwa ndi lilime la Davide ndi
la Yesu, mwana wa wamamuna wa Maria. Zimenezo ndi
chifukwa chakuti adanyoza ndi kulumpha malire. 79. Iwo
sanali kuletsana wina ndi mnzake kuchita zoipa zimene
ankachita. Ndithudi ndi zoipa zimene adali kuchita.
80. Iwe umawaona anthu ambiri akupalana ubwenzi ndi
anthu osakhulupirira. Ndithudi ndi zinthu zoipa zimene
iwo adatsogoza ndipo chifukwa cha ichi mkwiyo wa
Mulungu unagwa pa iwo ndipo adzalandira chilango
chosatha. 81. Ndipo iwo akadakhulupirira mwa Mulungu
ndi mwa Mtumwi ndi zimene zavumbulutsidwa kwa iye,
iwo sakadapalana nawo ubwenzi. Koma ambiri a iwo ndi
anthu ochita zoipa.
82. Ndithudi udzaona kuti anthu odana kwambiri ndi
anthu okhulupirira ndi Ayuda ndi anthu opembedza mafano
ndipo udzapeza amene amakhala kufupi pokondana ndi
anthu okhulupirira ndiwo amene amati: "Ndife Akhirisitu."
Chifukwa chake ndi chakuti pali pakati pawo Ansembe
ndi Abusa ndipo iwo sadzikweza. 83. Ndipo pamene iwo
amamvetsera ku zimene zavumbulutsidwa kwa Mtumwi,
udzaona misozi ili kuyengeza m'maso mwawo chifukwa
cha choonadi chimene adziwa. Iwo amati: "Ambuye wathu!

Ife takhulupirira motero tilembeni pamodzi ndi omwe
akuikira umboni.” 84. “Kodi ife tisakhulupirire bwanji mwa
Mulungu ndi chimene chadza kwa ife moonadi pamene ife
tikufunitsitsa kuti Ambuye wathu akatilowetse pamodzi
ndi anthu ochita zabwino?” 85. Motero, chifukwa cha zimene
ananena, Mulungu adawalipira minda yothiriridwa ndi
madzi ya m'mitsinje kumene adzakhaleko mpaka kalekale.
Amenewa ndiwo malipiro a anthu olungama. 86. Koma iwo
amene sanakhulupirire ndipo amakana chivumbulutso
chathu, iwo adzakhala eni ake aku Gahena.

87. Oh inu anthu okhulupirira! Musaletse zabwino zimene
Mulungu wakulolani kuti muchite, musadumphe malire.
Ndithudi Mulungu sakonda anthu odumpha malire.
88. Ndipo idyani zinthu zololedwa ndi zabwino zonse
zimene Mulungu wakupatsani ndipo opani Mulungu
amene inu mumakhulupirira. 89. Mulungu sadzakulangani
inu chifukwa cha kulumbira kwanu kosakonzekera. Koma
Iye adzakulangani chifukwa cha malonjezo anu a bodza.
Kulipira kwake ndi kudyetsa anthu khumi osowa ndi
chakudya chimene inu mumadyetsa banja lanu kapena
kuwaveka kapena kumasula kapolo mmodzi. Koma yense
amene sangathe kukwaniritsa china cha izi, ayenera kusala
masiku atatu. Kumeneko ndiko kulipira kwa malonjezo
anu ngati mwalumbira. Motero sungani malonjezo anu.
Mmenemo ndimo mmene Mulungu amaonetsera poyera
chivumbulutso chake kuti mukhale oyamika.

90. Oh inu anthu okhulupirira! Zoledzeretsa, masewera
a mwayi, kupembedza mafano ndi mipaliro ndi ntchito
zoipa zopangidwa ndi Satana. Motero zipeweni kuti
mukhale opambana. 91. Ndithudi cholinga cha Satana

ndikudzetsa udani pakati panu pogwiritsa ntchito
zoledzeretsa, masewera a mwayi ndiponso kukuletsani
inu kuti muzikumbukira Mulungu ndi mapemphero.
Kodi simungathe kuzisiya? 92. Ndipo mverani Mulungu
ndi Mtumwi. Chenjerani ndipo opani Mulungu. Ngati inu
mutembenuka dziwani kuti udindo wa Mtumwi wathu
ndi kupereka uthenga momveka. 93. Kwa onse amene
akhulupirira ndi kuchita zabwino sipadzakhala mlandu pa
nkhani ya chakudya chilichonse chimene adadya ngati iwo
aopa Mulungu, akhulupirira mwa Iye ndi kuchita ntchito
zabwino moyenera. Mulungu amakonda anthu ochita
zabwino.

94. Oh inu anthu okhulupirira! Mulungu adzakuyesani inu
ndi nyama zimene mukhoza kugwira ndi manja anu kapena
kupha ndi mikondo yanu kuti Mulungu awadziwe onse
amene amamuopa Iye mwamseri. Yense amene adumpha
malire pambuyo pa izi adzakhala ndi chilango chowawa.
95. Oh inu anthu okhulupirira! Musaphe nyama za m'thengo
pamene mutavala zobvala za Hajji kapena Umra. Yense wa
inu amene apha nyama mwadala, adzapereka, ngati dipo
lofika ku Kaaba, nyama yoweta yofanana ndi imene iye
wapha, imene idzatsimikizidwa ndi anthu awiri olungama
amene ali pakati panu kapena m'malo mwake adzadyetsa
anthu osauka kapena kusala kuti alawe kuipa kwa ntchito
zake. Mulungu wakhululukira zonse za m'mbuyo koma
ngati wina abwerera ku uchimo, Mulungu adzamulanga
kwambiri. Mulungu ndi wamphamvu ndipo ndi mwini
kubwezera.

96. Ndi chololedwa kwa inu kusodza m'nyanja ndi kudya
za mnyanja, inu ndi iwo a paulendo. Koma mwaletsedwa

kupha nyama za pa mtunda pamene mutabvala zobvala
za Hajji kapena Umra. Opani Mulungu kumene nonse
mudzasonkhanitsidwa. 97. Mulungu anapanga Ka'ba,
Nyumba yolemekezeka, malo a chitetezo ndi Hajji
ndi Umra, anthu ndiponso Miezi Yoyera ndi nyama
zoperekedwa ngati nsembe ndiponso zizindikiro zimene
amamangira pa izo, kuti mukhoza kudziwa kuti Mulungu
amadziwa zonse zimene zili mlengalenga ndi dziko lapansi
ndiponso kuti Mulungu amadziwa zonse. 98. Dziwani kuti
Mulungu ali ndi chilango chowawa ndipo kuti Mulungu
ndi wokhululukira ndi wachisoni chosatha. 99. Ntchito
ya Mtumwi ndi kungopereka chenjezo. Ndipo Mulungu
amadziwa zonse zimene mumaonetsa ndi zimene
mumabisa. 100. Nena: "Zabwino ndi zoipa sizifanana
ngakhale kuti kuchuluka kwa zoipa kumakusangalatsani
kwambiri." Opani Mulungu inu anthu ozindikira,kuti
mukhale opambana.

101. Oh inu anthu okhulupirira! Musamafunse
zinthu zimene ngati zitadziwika kwa inu zikhoza
kukuvutitsani. Koma ngati mufunsa za izo pamene
Korani ili kuvumbulutsidwa kwa inu, zidzafotokozedwa
mwatsatanetsatane kwa inu. Mulungu wakhululuka
ndipo Mulungu ndi wokhululukira ndi wopilira kwambiri.
102. Anthu ena, anafunsa za izo, inu musanadze koma iwo
adakhala osakhulupirira. 103. Si Mulungu amene adayambitsa
Bahira (miyambo yosakama ngamira yaikazi kapena Saiba
(ngamira yaikazi kuisiya yokha kuubusa) kapena Wasila
(kupereka nsembe ya nyama ya ngamila imene ibereka
ana akazi motsatizana) kapena Ham (mitheno ya ngamira
imene yaletsedwa kugwira ntchito) koma ndi anthu

osakhulupirira amene amapeka bodza lokhudza Mulungu ndipo ambiri a iwo alibe nzeru. 104. Pamene zinenedwa kwa iwo kuti: Bwerani ku chimene Mulungu wavumbulutsa ndi kwa Mtumwi. Iwo amati, "Chikhulupiriro chimene adatisiyira makolo athu ndi chotikwanira." Ngakhale kuti makolo awo samadziwa chilichonse ndipo sadatsogozedwe bwino. 105. Oh inu anthu okhulupirira! Dzisamaleni nokha. Iye amene wasokera sangakuchiteni kanthu kalikonse ngati inu muli ochita zabwino. Nonse mudzabwerera kwa Mulungu ndipo adzakuuzani zimene munali kuchita.

106. O inu anthu okhulupirira! Pamene imfa idza pa mmodzi wa inu panthawi yopereka mawu, anthu awiri olungama achitire umboni pakati panu; kapena anthu amuna awiri ochokera kumtundu wina osakhulupirira ngati muli paulendo padziko ndipo imfa yakupezani. Asungeni mpaka mutatha kupemphera ndipo ngati mukaika za kukhulupirika kwawo, afunseni kuti alumbire pali Mulungu kuti: "Ife sitigulitsa umboni wathu pamtengo wina uliwonse ngakhale kwa m'bale wathu weniweni. Ndipo ife sitibisa umboni wa Mulungu, ndithudi ife titatero tikhala mgulu la anthu ochimwa." 107. Koma ngati zidziwika kuti anthu awiriwa ali ndi mlandu wina, sankhulani anthu ena awiri kuti aime m'malo mwawo, amene ali a chibale a munthu amene ali kufa. Iwo ayenera kulumbira pali Mulungu kuti: "Ife titsimikiza kuti umboni wathu ndi woona kuposa wa anthu awiriwo ndipo kuti ife sitinaperekepo umboni wabodza ndipo ngati ife tinama, ndiye kuti ndife olakwa." 108. Imeneyo ndiyo njira yapafupi yoti iwo akhoza kupereka umboni woona weniweni poopa kuti ena akhoza kulumbira pambuyo pakulumbira kwawo. Muopeni Mulungu ndipo

mverani ulangizi wake. Mulungu satsogolera anthu ochita zoipa.

109. Patsiku limene Mulungu adzasonkhanitsa Atumwi ake onse ndi kuwafunsa kuti: "Kodi mudayankhidwa bwanji?" Iwo adzati: "Ife sitidziwa. Ndithudi Inu nokha ndiye amene mumadziwa zonse zimene ndi zobisika."
110. Pamene Mulungu adzati: "Oh! iwe Yesu, mwana wamwamuna wa Maria! Kumbukira zokoma zanga zimene ndinakhazikitsa pa iwe ndi pa amayi ako; mmene ndidakulimbitsa iwe ndi Mzimu Woyera moti udalankhula kwa anthu pamene unali wakhanda ndiponso utakula msinkhu; mmene ndidakuphunzitsira iwe mawu a Mulungu ndi kukuonjezera luntha labuku la chipangano chakale ndi chipangano chatsopano; mmene ndi chilolezo changa udapanga kuchokera kudothi, chinthu cholingana ndi mbalame ndipo udachiuzira mpweya ndipo ndi chilolezo changa, icho chidasanduka mbalame ya moyo; ndipo mmene ndi chilolezo changa udachiritsa anthu a khungu ndi anthu a makate ndiponso ndi chilolezo changa unali kupereka moyo kwa anthu akufa; mmene ndidakutetezera iwe kwa ana a Israyeli pamene udadza kwa iwo ndi zizindikiro zooneka," ndipo anthu osakhulupirira amene adali pakati pawo adati: "Ichi sichina chilichonse koma matsenga oonekera poyera."

111. Mmene ndidalamulira ophunzira ako kuti akhulupirire mwa Ine ndi mwa Mtumwi wanga, iwo adati: "Ife takhulupirira. Ndipo chitira umboni kuti ife tidzipereka kwathunthu kwa Mulungu." 112. Pamene ophunzira adati: "Oh iwe Yesu, mwana wamwamuna wa Maria! Kodi angathe, Ambuye wako, kutitumizira ife kuchokera

kumwamba gome lodzala ndi chakudya?" Iye adati:
"Muopeni Mulungu ngati inu ndinu okhulupirira." 113. Iwo
adati: "Ife tifuna kudya kuchokera pa ilo kuti mitima yathu
ikhazikike ndi kudziwa kuti zonse zimene udatiuza ife
ndi zoona, ndipo kuti ife tikhoza kukhala mboni wa izo."
114. Yesu, mwana wamwamuna wa Maria, adati: "Oh Ambuye
wathu! Titumizireni ife kuchokera kumwamba gome
lodzala ndi chakudya kuti likhale phwando lathu ndi la iwo
amene akudza mtsogolo; ndi chizindikiro chochokera kwa
inu. Ndipo tipatseni chakudya. Ndipo Inu ndinu Wabwino
mwa onse opereka." 115. Mulungu adati: "Ine nditumiza
gome kwa inu koma aliyense wa inu amene, ataona izi,
sadzakhulupirira ndidzamulanga ndi chilango chimene
sindidalangepo wina aliyense wa zolengedwa zanga."
116. Pamene Mulungu adzati: "O! iwe Yesu, mwana
wamwamuna wa Maria! Kodi udawauza anthu kuti:
Ndipembedzeni ine ndi Amai anga ngati milungu iwiri
powonjezera pa Mulungu?" Iye adzayankha: "Ulemerero
ukhale kwa Inu! Sikunali koyenera kuti ine ndinene zinthu
zimene ndinalibe ulamuliro wonenera. Ngati ndikadanena
choncho, ndithudi, inu mukadadziwa. Inu mumadziwa
zimene zili mumtima mwanga pamene ine sindidziwa
zimene zili mu mtima mwanu. Inu nokha mumadziwa
zinthu zobisika." 117. "Ine sindinawauze china chilichonse
kupatula zimene Inu mudandilamula kuti ndinene zoti.
'Pembedzani Mulungu, Ambuye wanga, amene ali Ambuye
wanu.' Ine ndidali mboni yawo pamene ndidali kukhala
pakati pawo koma pamene Inu mudanditenga ine kudza
kwa Inu, Inuyo ndiye amene mudali kuwayang'anira ndipo
Inu ndinu mboni pa zinthu zonse." 118. "Ngati muwalanga,

iwo ndi akapolo anu, koma ngati muwakhululukira, ndithudi, Inu ndinu wa mphamvu ndi Mwini nzeru.”
119. Ndipo Mulungu adzati: “Ili ndilo tsiku limene chilungamo chawo chidzawapindulira anthu olungama.” Iwo adzakhala nthawi zonse m’minda yothiriridwa ndi mitsinje yamadzi yoyenda pansi pake. Iwo adzakhalamo mpaka kalekale. Mulungu ndi osangalala ndi iwo ndipo iwo ndi Iye. Kumeneku ndiko kupambana kwakukulu.
120. Mulungu ndiye mwini wa Ufumu wa kumwamba ndi dziko lapansi ndi zonse zimene zili m’menemo ndipo Iye ali ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse.

Sura 6 • Al-An‘âm

## Al – Anam

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Kuyamikidwa ndi kwa Mulungu amene adalenga kumwamba ndi dziko lapansi ndi kukhazikitsa mdima ndi kuwala, komabe anthu osakhulupirira amakhazikitsa milungu ina kuti ndi yolingana ndi Ambuye wawo.
2. Iye ndiye amene adakulengani inu kuchokera ku dothi ndipo Iye adakhazikitsa nthawi. Ndipo Iye adakhazikitsanso nthawi ina, komabe inu mumakaika.
3. Iye ndi Mulungu wa kumwamba ndi dziko lapansi. Iye amadziwa zonse zimene mumabisa ndi zonse zimene mumaulula. Ndipo amadziwa zimene mumachita.
4. Ndipo chizindikiro sichidza kwa iwo kuchokera ku zizindikiro za Ambuye wawo, chimene

iwo amachivomereza. 5. Ndithudi iwo adakana choonadi
pamene chidadza kwa iwo; koma kudzadza kwa iwo
nkhani za zimene adali kuchita chipongwe. 6. Kodi iwo
sadaone kuti kodi ndi mibadwo ingati, iwo asanabadwe,
imene Ife tidawononga imene tidakhazikitsa pa dziko
kukhala ya mphamvu kwambiri kuposa inu? Ndipo
timawatumizira mvula yochuluka kuchokera kumwamba
ndi kuipanga mitsinje yamadzi kuyenda pansi pawo.
Komabe tidawawononga chifukwa cha machimo awo
ndipo tidalenganso, pambuyo pa iwo, mibadwo ina.
7. Ngakhale Ife tikadakutumizira iwe uthenga
wolembedwa kale papepala kuti alikhudze ndi manja awo,
anthu osakhulupirira akadanena kuti: "Ichi si china ayi
koma matsenga enieni." 8. Iwo adati: Kodi ndi chifukwa
chiyani mngelo sadatumizidwe kwa iye? Ife tikadatumiza
mngelo, nkhani ikanaweruzidwa nthawi yomweyo, ndipo
sakadapatsidwa mpata. 9. Ndipo ngati Ife tikadamupanga
iye kukhala mngelo, ndithudi Ife tikadamupanga iye kuti
azioneka ngati munthu ndipo tikadawasokoneza ndi
zimene iwo adasokonezeka nazo kale. 10. Ndipo, ndithudi,
Atumwi ena adasekedwa iwe usadadze, koma amene anali
kuwaseka anazungulilidwa ndi zinthu zomwe iwo anali
kuseka. 11. Nena: "Yendani pa dziko lapansi ndipo muone
mapeto a anthu amene anakana choonadi."
12. Nena: "Kodi mwini wa chilichonse chimene chili
kumwamba ndi dziko lapansi ndani?" Nena: "Mwini wake
ndi Mulungu" ndipo Iye adadzilamula yekha kuti azionetsa
chifundo. Ndipo, ndithudi, Iye adzakusonkhanitsani
nonse pa tsiku la kuuka kwa akufa, tsiku lopanda chikaiko.
Iwo amene asochera sadzakhulupirira. 13. Ndipo zake ndi

zonse zimene zimapezeka usiku ndi usana ndipo Iye ndi
Wakumva ndi Wozindikira. 14. Nena: “Kodi ine nditenge
wina aliyense osati Mulungu kuti akhale Mtetezi wanga,
Mlengi wakumwamba ndi dziko lapansi? Iye ndiye amene
amadyetsa pamene Iye sadyetsedwa.” Nena: “Ndithudi
ine ndalamulidwa kukhala woyamba wa anthu ogonjera
kwa Mulungu.” Iwe usadzakhale mmodzi wa iwo amene
amapembedza mafano. 15. Nena: “Ine ndikuopa, ngati
nditanyoza Ambuye wanga, chilango cha tsiku lalikulu.”
16. Aliyense amene adzapulumutsidwa ku mazunzo a tsiku
limeneli adzakhala atalandira chifundo cha Mulungu.
Kumeneko ndiko kudzakhala kupambana kwenikweni
koonekeratu.

17. Ndipo ngati Mulungu akupatsa mavuto, palibe wina
amene angachotse mavutowo koma Iye yekha; ndipo
ngati Iye akupatsa zinthu zabwino, Iye ali ndi mphamvu
pa chinthu china chilichonse. 18. Iye ali ndi mphamvu pa
akapolo ake ndipo Iye ndiye Wanzeru ndi Wodziwa zonse.
19. Nena: “Kodi ndi chiani chili chachikulu mu umboni?”
Nena: “Mulungu ndiye mboni pakati pa ine ndi inu. Buku la
Korani lavumbulutsidwa kwa ine kuti ndikuchenjezeni inu
ndi ena onse amene angalandire chivumbulutsochi. Kodi
inu mungachitire umboni kuti pali milungu ina yoonjezera
pa Mulungu weniweni?” Nena: “Ine sindingaikire umboni
pa nkhani yotere.” Nena: “Iye ndi Mulungu mmodzi yekha.
Ndipo, ndithudi, ine ndili kutali ndi milungu imene inu
muli kupembedza powonjezera pa Iye.”

20. Kwa iwo amene tidawapatsa Buku amamudziwa Iye
monga momwe amadziwira ana awo. Koma iwo amene ataya
mizimu yawo sadzakhulupirira. 21. Kodi wolakwa kwambiri

ndani kuposa munthu amene amapeka bodza lokhudza
Mulungu kapena amakana chivumbulutso chake? Ndithudi
anthu ochita zoipa sadzapambana ayi. 22. Ndipo patsiku
limene tidzawasonkhanitsa onse pamodzi, Ife tidzati kwa
anthu opembedza mafano: “Kodi ali kuti mafano anu aja
munkawadalira?” 23. Iwo sadzawiringula china chili chonse
koma adzati: “Tilumbira pali Mulungu, Ambuye wathu,
kuti ife sitidali kupembedza mafano pambali pa Mulungu.”
24. Taona mmene iwo ali kudzinamiza okha! Koma bodza
limene anali kupeka lidzawathawira.

25. Ndipo ena a iwo amamvetsera kwa iwe koma Ife
taika tchingo m’mitima mwawo kuti asazindikire ndipo
m’makutu mwawo ndi mogontha ndipo iwo akaona
chizindikiro chilichonse, sadzachikhulupirira ndipo
amadza kwa iwe kudzatsutsana nawe, ndipo anthu
osakhulupirira amati: “Ichi sichina chilichonse koma
nkhani zopeka za anthu a kale kwambiri.” 26. Ndipo iwo
amaletsa anthu kumvetsera ndipo iwo amadzitalikitsa
okha kwa Iye. Koma iwo sali kuwononga wina aliyense
koma akudziononga okha. Koma iwo sazindikira. 27. Koma
iwe ukadawaona pamene iwo adzaimitsidwe moyandikira
moto! Iwo adzati: “Zikadakhala kuti tinabwezedwa! Ife
sitikadakana chivumbulutso cha Ambuye wathu ndipo
tikadakakhala anthu okhulupirira.” 28. Koma zonse zimene
adali kuzibisa kale zidzaonekera poyera kwa iwo. Komabe
akadabwezedwa, iwo akadakabwerera ku zinthu zimene
adaletsedwa. Ndithudi iwo ndi anthu a bodza.

29. Iwo adanenetsa kuti: “Kulibenso moyo wina uliwonse
kupatula moyo wathu wadziko lapansi ndiponso ife
sitidzaukitsidwa kwa akufa.” 30. Ndipo iwe ukadawaona

pamene ali kusonkhanitsidwa kuima pamaso pa Ambuye
wawo! Iye adzati: "Kodi izi sizoona?" Iwo adzayankha: "Ndi
zoona pali Ambuye wathu." Ndipo Iye adzati: "Motero
lawani chilango chifukwa inu simunali okhulupilira."
31. Ndithudi iwo ndi olephera kwambiri amene amakana
kuti adzakumana ndi Ambuye wawo mpaka pamene ola
loopsa lidza pa iwo mwadzidzidzi ndipo iwo adzafuula
kuti: "Kalanga ife tidali kunyalanyaza kwambiri!" Iwo
adzanyamula katundu wawo pa misana yawo ndipo zoipa
kwambiri zimene adzasenza. 32. Ndipo moyo wa padziko lino
lapansi siuli kanthu konse koma masewera ndi nthabwala.
Koma yabwino kwambiri ndi nyumba m'moyo umene uli
nkudza kwa amene amaopa. Kodi simungazindikire?
33. Ife tili kudziwa kuti zonse zimene ali kunena zili
kukukhumudwitsa. Sindiwe amene iwo ali kukana koma
ndi chivumbulutso cha Mulungu chimene anthu ochita
zoipa ali kukana. 34. Ndithudi Atumwi ena adakanidwa iwe
usanadze koma iwo adapilira pa zimene adali kuwanena
ndipo anazunzidwa mpaka pamene thandizo lathu lidadza
kwa iwo ndipo palibe amene angasinthe chilamulo cha
Mulungu. Ndithudi iwe udamva nkhani za Atumwi. 35. Ngati
uona kuti kukana kwawo kwanyanya ndipo kuti sungathe
kupirira, peza ngati ungathe, njira yapansi pa nthaka
kapena makwerero oti ukwere kumwamba, kuti ukhoza
kuwabweretsera chizindikiro. Ngati Mulungu akadafuna,
Iye akadawasonkhanitsa onse ku chilangizo choona ndipo
iwe usakhale mmodzi wa mbuli. 36. Ndi okhawo amene
amamva, amene adzapindula koma anthu akufa Mulungu
adzawadzutsa kwa akufa ndipo kwa Iye adzabwerera.
37. Iwo amafunsa: "Kodi ndi chifukwa chiyani chizindikiro

sichinadze kwa iye kuchokera kwa Ambuye wake?”
Nena: “Ndithudi Mulungu ali ndi mphamvu zotumiza
chizindikiro koma ambiri a iwo sazindikira.” 38. Palibe
chinthu cha moyo padziko lapansi kapena mbalame imene
imauluka ndi mapiko ake awiri imene ndi zosiyana ndi
inu. Ife sitidasiye china chilichonse m’Buku ndipo kwa
Ambuye wawo iwo adzasonkhanitsidwa. 39. Koma iwo
amene amakana zizindikiro zathu, ndi agonthi m’khutu ndi
abububu mu mdima. Mulungu amasocheza aliyense amene
Iye wamufuna ndipo amatsogolera, kunjira yoyenera,
aliyense amene Iye wamufuna.

40. Nena: “Ndiuzeni, ngati chilango cha Mulungu
chitadza pa inu kapena ola loopsa lidza pa inu, kodi
inu mudzapempha wina amene sali Mulungu kuti
akuthandizeni inu? Yankhani ngati mukunena zoona.”
41. Iyayi! Ndi kwa Iye yekha kumene inu mumapempha
ndipo ngati Iye atafuna akhoza kukuchotserani zovuta
zanu, ndipo inu pa nthawi imeneyi mudzaiwala mafano
anu.

42. Ndithudi Ife tidatumiza, iwe usanadze, Atumwi
ku mitundu ina. Ndipo tidawagwetsera umphawi,
matenda ndi matsoka ochuluka kuti akhoza
kukhulupilira modzichepetsa. 43. Nanga ndi chifukwa
chiyani iwo sadadzichepetse pamene mazunzo athu
adadza pa iwo? Koma mitima yawo inalimba ndipo
Satana adawakongoletsera zochita zawo zoipa zimene
adali kuchita. 44. Ndipo pamene iwo adaiwala zimene
adachenjezedwa, Ife tidawatsegulira makomo a zinthu
zonse zabwino mpaka pamene adasangalala ndi zimene
adapatsidwa, mwadzidzidzi Ife tidawalanga ndipo ah!

Iwo adalowa m'chionongeko wokhumudwa ndi a chisoni.
45. Motero maziko a anthu ochimwa adaonongedwa. Ndipo
kutamandidwa konse kukhale kwa Mulungu, Ambuye wa
zolengezedwa zonse.
46. Nena: "Tandiuzani! Ngati Mulungu akadakulandani
kumva kwanu, kuona kwanu ndi kutseka mitima yanu,
kodi pali mulungu wina, woonjezera pa Mulungu
weniweni, amene angakubwezereni zimenezi?" Taonani
mmene tifotokozera chivumbulutso chathu ndi mmene
iwo sakhulupilira. 47. Nena: "Ndiuzeni, ngati chilango
cha Mulungu chitadza mwadzidzidzi kapena moonekera,
kodi ndani angaonongeke kupatula anthu ochita zoipa?"
48. Ndipo Ife sititumiza Aneneri koma kuti azikawauza
anthu nkhani yabwino ndi kuwachenjeza. Motero aliyense
amene akhulupirira ndi kuchita ntchito zabwino, iye
sadzakhala ndi nkhawa kapena kudandaula. 49. Koma
iwo amene akana chivumbulutso chathu, chilango
chidzawapeza chifukwa cha kusakhulupilira kwawo.
50. Nena: "Ine sindili kukuuzani kuti ndili ndi chuma cha
Mulungu kapena kuti ndimadziwa zinthu zobisika kapena
kuti ine ndine mngelo. Ine sinditsatira china chilichonse
kupatula zokhazo zimene zavumbulutsidwa kwa ine."
Nena: "Kodi munthu wakhungu ndi munthu openya
angafanane? Kodi inu simungaganize?"
51. Ndipo achenjeze iwo amene amaopa kuti
adzasonkhanitsidwa kupita kwa Ambuye wawo, amene
alibe wowasamalira kapena mkhalapakati woonjezera
pa Mulungu, kuti akhoza kumalewa zoipa. 52. Ndipo
usawathamangitse iwo amene amapembedza Ambuye
wawo m'mawa ndi madzulo pofuna chisangalalo chake. Iwe

siudzaimbidwa mlandu pa zochita zawo ndipo nawonso
sadzaimbidwa mlandu pa zochita zako ndipo ngati iwe
uwathamangitsa udzakhala mugulu la anthu opanda
chilungamo. 53. Motero ife tinawayesa ena a iwo kupyolera
mwa anzawo kuti akhoza kunena, “Kodi awa ndiwo amene
Mulungu wawadalitsa pakati pathu?” Kodi Mulungu
sazindikira anthu othokoza?

54. Ngati atadza kwa iwe anthu amene amakhulupirira
chivumbulutso chathu. Nena, “Mtendere ukhale pa inu.”
Ambuye wanu adadzilamulira yekha kuti azionetsa chisoni
kuti ngati wina wa inu achita choipa chifukwa chosadziwa
ndipo alapa pambuyo pake ndipo achita ntchito zabwino,
ndithudi Iye ndi wokhululukira ndi wachisoni chosatha.
55. Motero Ife timafotokoza chivulumbutso chathu poyera
kuti njira ya anthu ochita zoipa ionekere poyera.

56. Nena, “Ine ndaletsedwa kupembedza milungu imene
inu mumaipembedza powonjezera pa Mulungu.” Nena, “Ine
sindidzatsatira zilakolako zanu zachabe. Ngati nditatero
ndiye kuti ndasochera ndipo ine sindikhala mugulu la anthu
otsogozedwa bwino.” 57. Nena, “Ine ndalandira umboni
wokwana kuchokera kwa Ambuye wanga komabe inu muli
kuukana. Ine ndilibe mphamvu yobweretsa msangamsanga
chilango chimene mufuna. Chiweruzo chili m’manja mwa
Mulungu yekha, Iye amanena zoona ndipo ndi yekhayo
amene ali wabwino poweruza.” 58. Nena, “Ine ndikadakhala
nacho chimene mufuna mwamsanga msanga, mkangano
wa pakati pa inu ndi ine ukadaweruzidwa kalekale koma
Mulungu amadziwa anthu onse ochita zoipa.” 59. Iye ali
ndi makiyi a zinthu zonse zobisika, palibe wina amene
azidziwa koma Iye yekha. Iye amadziwa zonse zimene zili

m'nthaka ndiponso m'nyanja; ndipo lisadagwe tsamba Iye
amalidziwa. Palibe mbewu mu mdima wa nthaka kapena
china chilichonse cha chiwisi kapena chouma koma
zonsezo zidalembedwa mu Buku looneka bwino.
60. Iye ndiye amene amachotsa mizimu yanu nthawi
yausiku ndipo amadziwa zonse zimene mwachita masana
ndipo amakudzutsani kuti mukwaniritse nthawi imene
idaperekedwa pa moyo wanu ndipo pambuyo pake nonse
mudzabwerera kwa Iye. Ndipo Iye adzakuuzani zonse
zimene mumachita. 61. Iye ndi wamphamvu pa akapolo ake
ndipo amatumiza atetezi amene amakuyang'anirani inu
mpaka pamene mmodzi wa inu imufikira imfa; Atumiki
athu amachotsa moyo wake ndipo iwo sanyoza zimene
alamulidwa. 62. Ndipo iwo amabwerera kwa Mulungu,
Ambuye wawo woona. Ndithudi Iye ndiye muweruzi
ndipo Iye ndi wachangu powerengera zochita zanu.
63. Nena, "Kodi ndani amakupulumutsani m'mavuto a pa
mtunda ndi a pa nyanja ndi pamene inu mumamupempha
Iye modzichepetsa ndi mwamseri, ponena kuti: 'Ngati Iye
atipulumutsa ife pa mavuto awa, ndithudi, ife tidzakhala
othokoza." 64. Nena, "Mulungu amakupulumutsani
inu ku zovuta izi ndi kumavuto ena onse, komabe inu
mumapembedzabe mafano mowonjezera pa Iye." 65. Nena,
"Iye ali ndi mphamvu yotumiza chilango chake pa inu
kuchokera pamutu panu kapena pansi pa mapazi anu kapena
kukugawani inu kukhala m'magulu a anthu osagwirizana
ndi kukulawitsani mazunzo ochokera kwa anzanu. Taonani
mmene timaonetsera poyera chivumbulutso chathu kuti
akhale ozindikira." 66. Koma anthu ako alikana ili ngakhale
lili choonadi chenicheni. Nena: "Ine sindine Msungi

wanu ayi.” [67.] Nkhani iliyonse ili ndi nthawi yake ndipo posachedwapa mudzazindikira.

[68.] Ndipo pamene iwe uwaona iwo amene amanyoza chivumbulutso chathu, usakhale nawo pamodzi mpaka pokhapokha akamba nkhani ina. Ngati satana akuiwalitsa, ndipo pambuyo pake ukumbukira usakhale mgulu la anthu ochita zoipa. [69.] Iwo amene amaopa Mulungu alibe udindo pa iwo koma kungowakumbutsa kuti apewe kunyoza. [70.] Apewe iwo amene amasandutsa chipembedzo chawo kukhala masewera kapena nthabwala ndipo asokonezeka ndi zokoma za moyo wa dziko lapansi. Koma achenjeze ndi ilo kuti ungadzaonongeke mzimu wawo chifukwa cha zimene udachita pamene siudzakhala ndi wousamalira kapena kuwuteteza kupatula Mulungu, ndipo ngakhale iwo apereka chuma chopepesera, sichidzalandiridwa konse. Otere ndiwo amene aonongedwa chifukwa cha zimene anachita. Iwo adzalandira zakumwa zowira ndi chilango chowawa chifukwa cha zinthu zimene sadakhulupirire.

[71.] Nena, “Kodi ife tizipembedza ena powonjezera pa Mulungu amene sangathe kutithandiza kapena kutiwononga ndipo kodi ife tibwerere m’mbuyo pamene Mulungu watitsogolera? Monga ngati munthu amene alodzedwa ndi Satana, kumangoyenda uku ndi uku ngakhale kuti abwenzi ake ali kumuitana kuti atsatire njira yoyenera, ponena: Bwerani kuno?” Nena, “Ndithudi utsogoleri wa Mulungu ndiwo utsogoleri weniweni ndipo Ife talamulidwa kugonjera Mulungu Ambuye wa zolengedwa zonse.” [72.] Ndi kuti muzipemphera moyenera, kumvera Mulungu ndi kumuopa Iye ndipo ndi kwa Iye kumene nonse mudzasonkhanitsidwa. [73.] Iye ndiye amene

adalenga kumwamba ndi dziko lapansi mwachoonadi ndipo
patsikuli Iye adzati: “Khala” ndipo chidzakhala. Liwu
lake ndi loonadi. Wake udzakhala Ufumu pa tsiku limene
lipenga lidzaombedwa. Iye amadziwa zonse zosaoneka
ndi zooneka. Iye ndi wanzeru ndi wodziwa zinthu zonse.
74. Ndi pamene Abrahamu adati kwa abambo ake a Uzar:
“Kodi inu muzipembedza mafano ngati milungu yanu?
Ndithudi ine ndili kuona kuti inu pamodzi ndi anthu anu
mwasochera moonekera.”
75. Motero tidamuonetsa Abrahamu Ufumu wa
kumwamba ndi wa dziko lapansi kuti akhale mmodzi
wa wokhulupirira kweniweni. 76. Ndipo pamene usiku
udamukuta ndi mdima, iye adaona nyenyezi. Iye adati:
“Iyo ndiyo Ambuye wanga.” Koma pamene iyo idalowa,
iye adati: “Ine sindikonda zimene zimalowa.” 77. Ndipo
pamene iye adaona mwezi uli kutuluka, iye adati: “Uwo
ndiwo Ambuye wanga.” Koma pamene iwo unalowa, Iye
adati: “Ngati Ambuye wanga sanditsogolera ine, ndithudi,
ine ndidzakhala m’gulu la anthu osochera.” 78. Ndipo
pamene adaona dzuwa lili kutuluka, iye adati: “Ili ndilo
Ambuye wanga. Ndipo ilo ndi lalikulu koposa.” Koma
pamene ilo lidalowa, iye adati: “Oh inu anthu anga! Ine
ndatalikirana ndi zimene inu mukusakaniza popembedza
Mulungu.” 79. Ndithudi ine ndayang’anitsa nkhope yanga
kwa Iye amene adalenga kumwamba ndi dziko lapansi. Ine
sindine mmodzi wa iwo opembedza mafano. 80. Anthu ake
adatsutsana naye ndipo iye adati: “Kodi inu mukutsutsana
ndi ine za Mulungu pamene Iye wanditsogolera? Ndipo
ine sindiopa mafano anu kupatula ngati Ambuye wanga
atafuna chilichonse. Ambuye wanga amadziwa bwino

chilichonse. Kodi inu simungakumbukire? 81. Ndipo kodi ine ndingaope bwanji milungu yanu yabodza pamene inuyo mulibe mantha pomapembedza mafano amene Mulungu sadakupatseni umboni wake? Kodi ndani wa magulu awiriwa amene afuna chitetezo ngati inu mumadziwa?” 82. Ndiwo amene ali okhulupirira ndipo sasakaniza chikhulupiriro chawo pochita ntchito zoipa, kwa iwo kuli mtendere ndipo ndi otsogozedwa. 83. Chimenechi chinali chizindikiro chathu chimene tidamupatsa Abrahamu kuti agonjetsere anthu ake. Ife timakweza wina aliyense amene tamufuna. Ndithudi Ambuye wako ndi wanzeru ndi wodziwa zinthu zonse. 84. Ndipo tidamupatsa iye Isake ndi Yakobo, aliyense tidamutsogolera ndipo iye asanadze, tidatsogolera Nowa ndipo pakati pa adzukulu wake Davide, Solomoni, Yobu, Yosefe, Mose ndi Aroni. Motero ndi mmene timalipirira anthu ochita abwino.

85. Ndi Zakariya, Yohane, Yesu, ndi Eliya, aliyense adali wangwiro. 86. Ndi Ishimayeli, Elisa, Yona ndi Loti, onsewa tidawalemekeza pakati pa zolengedwa zonse. 87. Ndiponso makolo awo, ana awo, ndi abale awo Ife tidawasankha ndi kuwatsogolera ku njira yoyenera. 88. Ichi ndi chilangizo cha Mulungu chimene amalangiza nacho aliyense amene wamufuna wa akapolo ake. Koma iwo akadatumikira milungu ina yoonjezera pa Mulungu m’modzi, ntchito zawo zonse zikadakhala zopanda phindu. 89. Awa ndi amene tidawapatsa Buku, chiweruzo ndi Utumwi. Koma ngati awa sakhulupirira mwa ilo, ndithudi Ife tawapatsa iwo amene akhulupilira mwa ilo. 90. Amenewa ndi anthu amene Mulungu adawatsogolera. Choncho tsatira chilangizo chawo. Nena, “Ine sindili kufuna malipiro chifukwa cha

ntchito iyi ayi. Ili ndi chenjezo kwa zolengedwa zonse."
91. Iwo sadapereke ulemu woyenera Mulungu pamene
adati: "Mulungu sadavumbulutse china chilichonse kwa munthu." Nena, "Kodi ndani yemwe adavumbulutsa Buku limene Mose anabwera nalo, muuni ndi chilangizo kwa anthu onse; amene mwalemba pa mipukutu ya mapepala, kuulula zina ndi kubisa zambiri? Ndipo mudaphunzitsidwa zimene inu ndiponso makolo anu sadazidziwe ndi kale lomwe." Nena: "Ndi Mulungu." Ndipo asiye okha kuti abadzisangalatsa ndi nkhani zopusa.

92. Ndipo ili ndi Buku lodalitsika limene tavumbulutsa,
kuchitira umboni zimene zinadza ilo lisadadze kuti uchenjeze Mzinda wa Makka ndi iwo amene amakhala mouzungulira. Iwo amene ali ndi chikhulupiriro mu zamoyo umene uli nkudza amakhulupirira ilo ndipo
amasamala kwambiri m'mapemphero awo. 93. Kodi
wolakwa kwambiri ndani kuposa iye amene amapeka bodza lonamizira Mulungu kapena amati: "Ine ndalandira chibvumbulutso pamene sichidavumbulutsidwe kwa iye chilichonse?" Kapena munthu amene amati: "Ine ndikhoza kuvumbulutsa zinthu zofanana ndi zimene Mulungu wavumbulutsa?" Ndipo iwe ukadangoona anthu ochimwa pamene ali kufa ndi pamene angelo ali kutambasula manja awo akuti: "Perekani mizimu yanu. Inu mudzalipidwa mphotho yochititsa manyazi lero chifukwa cha zimene munali kunena zabodza zokhudza Mulungu. Ndiponso inu munali kukana chivumbulutso chake mwa mwano."

94. "Ndipo, ndithudi, mwadza kwa Ife, nokha, monga
momwe tidakulengerani inu poyamba. Inu mwasiya zonse zimene tidakupatsani kumbuyo kwanu. Ndiponso Ife sitili

kuona pamodzi ndi inu zimene mumazipembedza, zija
mumati ndi zofanana ndi Mulungu. Tsopano ubale wonse
umene umakugwirizitsani waduka ndipo zonse zimene
mumaziganizira kuti zingakuthandizeni zakuthawirani.”
95. Ndithudi! Ndi Mulungu amene amasiyanitsa mbewu ndi
khoko lake kuti imere. Iye amatulutsa chamoyo kuchokera
mu chakufa ndipo ndiye amatulutsa chakufa kuchokera ku
chamoyo. Ameneyo ndiye Mulungu, nanga ndi chifukwa
chiyani mukusokera kusiya choonadi?

96. Iye amadzetsa kuwala kwa m’mawa. Ndipo Iye
waika usiku kuti ikhale nthawi yopumula, dzuwa ndi
mwezi kuti zikhale zothandiza kuwerengera; umenewo
ndiwo muyeso wa Mwini mphamvu zonse ndi wodziwa
chilichonse. 97. Iye ndiye amene adakulengerani nyenyezi
kuti zizikutsogolerani mu mdima wa pa mtunda ndi pa
nyanja. Ife tafotokoza chivumbulutso kwa anthu odziwa
kwambiri. 98. Iye ndiye amene adakulengani inu kuchokera
kwa munthu mmodzi ndipo adakupatsani malo okhalamo
ndi osungidwa. Ife ndithudi tafotokoza chivumbulutso
chathu kwa anthu omvetsa.

99. Iye ndiye amene amatumiza mvula kuchokera
kumwamba ndipo ndi iyo, Ife timameretsa mbewu
zosiyana siyana ndipo kuchokera ku izo timatulutsa mphesi
za ziwisi zimene zimabereka mbeu mothinana. Ndipo
kuchokera ku mitengo ya tende kumadza zipatso za tende
zotsika pansi, minda ya mphesa ndi mitengo ya mafuta
ya azitona, chimanga cha chizungu, zipatso zofanana
koma zosiyanasiyana. Taonani zipatso zake pamene zili
kubereka, kukhwima ndi kumapsya. Ndithudi! Mu izi
muli zizindikiro kwa anthu okhulupirira. 100. Komabe iwo

amasankha majini kukhala milungu kuonjezera pa Mulungu
weniweni ngakhale kuti Iye ndiye amene anawalenga
ndipo amamunamizira Mulungu kuti ali ndi ana amuna
ndi akazi. Ulemerero ukhale kwa Iye! Alemekezeke Iye
koposa zonse zimene akunena! 101. Iye ndi Namalenga
wa kumwamba ndi dziko lapansi. Kodi Iye angakhale ndi
ana bwanji pamene Iye alibe mkazi? Iye adalenga zinthu
zonse ndipo amadziwa chilichonse 102. Ameneyo ndiye
Mulungu, Ambuye wanu. Kulibe Mulungu wina koma Iye
yekha, Namalenga wa zinthu zonse. Motero mpembedzeni
Iye yekha. Iye ndiye wosamalira zinthu zonse. 103. Palibe
amene angamuone Iye koma Iye amaona chili chonse. Iye
ndiye wachifundo ndipo amadziwa zonse. 104. Ndithudi
zizindikiro zonse zadza kwa inu kuchokera kwa Ambuye
wanu ndipo aliyense amene aona zidzampindulira iye
koma aliyense amene ali wakhungu adzalephera yekha
ndipo ine sindine wokuyang'anirani. 105. Motero Ife
timafotokoza chivumbulutso chathu, kuti iwo anene kuti:
"Iwe waphunzira" ndi kuti tifotokoze momveka kwa anthu
ozindikira.

106. Choncho tsatira zonse zimene zavumbulutsidwa
kwa iwe kuchokera kwa Ambuye wako. Kulibe Mulungu
wina koma Iye yekha ndipo alewe anthu osakhulupirira.
107. Ngati Mulungu akadafuna, iwo sakanapembedza
mafano. Ndipo Ife sitikadakusankha iwe kukhala
owayang'anira ayi ndiponso iwe sindiwe wowasamalira
wawo. 108. Ndipo musatukwane iwo amene amapembedza
mafano poonjezera pa Mulungu weniweni kuti mwina iwo
angathe kutukwana Mulungu molakwa ndi mwa umbuli.
Motero tazipanga zochita zawo kukhala zosangalatsa

ndipo ndi kwa Ambuye wawo kumene onse adzabwerera ndipo Iye adzawauza iwo zonse zimene anali kuchita. 109. Ndipo iwo amalumbira pali Mulungu motsindika kuti ngati chizindikiro chitaperekedwa kwa iwo, iwo adzachikhulupirira. Nena, "Ndithudi zizindikiro zonse zili ndi Mulungu ndipo kodi inu mungadziwe bwanji ngati chidza kwa iwo kuti iwo sadzachikhulupirira?"

110. Ndipo Ife tidzatembenuza mitima yawo ndi maso awo monga mmene adakana kukhulupirira nthawi yoyamba ndipo Ife tidzawasiya mukusochera kwawo akusowa chochita. 111. Ngakhale Ife tikadawatumizira iwo angelo ndi kupanga anthu akufa kuti alankhule nawo ndi kusonkhanitsa zinthu zonse pamaso pawo, iwo sakadakhulupirirabe pokhapokha ngati Mulungu afuna koma ambiri a iwo ndi anthu osadziwa. 112. Kotero Ife tidakhazikitsa mdani kwa Mtumwi aliyense. A satana amene ali pakati pa anthu ndi majini, amene amauzana wina ndi mnzake mawu okoma ndiponso a chinyengo. Koma Ambuye wako akadafuna, iwo sakadachita zotero ayi motero asiyeni okha ndi zimene akupeka. 113. Kuti mitima ya anthu amene sakhulupirira m'moyo umene uli nkudza ipendekere kuzolankhula zawo ndipo kuti azitsatira zimene apeka okha ndi kumasangalala kuti mwina akhoza kuchita zimene ali nkuchita. 114. "Kodi ine ndifune wina woweruza oposa Mulungu pamene ndiye amene adavumbulutsa Korani kwa inu ndi malamulo ofotokozedwa bwino?" Iwo amene tidawapatsa Mau athu amadziwa kuti lidavumbulutsidwa kuchokera kwa Ambuye wako mwa choonadi. Motero usakhale mmodzi wa anthu okaika.

115. Ndipo Mau a Ambuye wako akwaniritsidwa moona

ndi mwachilungamo. Palibe wina amene angasinthe Mau
ake. Iye amamva ndipo ndi wozindikira chili chonse.
116. Ndipo ngati iwe umvera zonena za anthu ambiri apa
dziko lapansi iwo adzakusocheza ku njira ya Mulungu.
Iwo satsatira chilichonse koma nkhani zongoganiza chabe
ndipo sachita china chilichonse koma kunama. 117. Ndithudi
Ambuye wako! Ndiye amene amadziwa anthu onse amene
amasochera ku njira yake ndiponso Iye amadziwa iwo
amene atsogozedwa bwino bwino. 118. Motero idyani
nyama yokhayo imene yaphedwa m'dzina la Mulungu ngati
inu mukhulupiriradi mu chivumbulutso chake.
119. Kodi inu simungadye bwanji nyama imene yaphedwa
m'dzina la Mulungu pamene Iye adaulula poyera zimene
adakuletsani pokhapokha ngati mwasimidwa? Ndithudi
ambiri amasochera potsatira zilako lako zawo mwa umbuli.
Ndithudi Ambuye wako amadziwa onse oswa malamulo.
120. Pewa machimo oonekera kapena obisika. Ndithudi
iwo amene amachita zoipa adzalangidwa chifukwa cha
zoipa zawo. 121. Musadye nyama iliyonse imene sidaphedwe
m'dzina la Mulungu chifukwa kutero ndi kulakwa. Ndithudi
a Satana amaphunzitsa anthu awo kuti azikangana ndi
inu ndipo ngati inu muwamvera, ndithudi, nanunso
mudzakhala opembedza mafano. 122. Kodi munthu amene
adafa, ndipo tamuukitsa kwa akufa ndipo wapatsidwa
kuwala kumene kukhoza kumutsogolera pakati pa anthu,
angafanizidwe ndi iye amene ali kusochera mumdima
umene sadzatulukamo? Chomwecho zimakongoletsedwa
kwa anthu osakhulupirira zimene adali kuchita.
123. Motero Ife tidakhazikitsa mu Mzinda uliwonse
atsogoleri a anthu olakwa kwambiri amene amakonza

njira zoswera malamulo m'kati mwa Mzindawo. Koma iwo amakonza njira zoti zibweretse chiwonongeko pa iwo eni ndipo iwo sadziwa. [124.] Ndipo pamene zizindikiro ziwafikira iwo amati: "Ife sitidzakhulupirira mu ichi pokhapokha ngati tipatsidwa chimene Atumwi a Mulungu adapatsidwa." Mulungu amadziwa bwino ndani amene akhoza kumupatsa uthenga wake. Kunyozedwa ndi kuchititsidwa manyazi kochokera kwa Mulungu ndiponso chilango chowawa chidzadza pa anthu oipa chifukwa cha zimene anali kuchita. [125.] Ndipo aliyense amene Mulungu afuna kumutsogolera, Iye amatsegula mtima wake kuti akhale Msilamu ndipo aliyense amene Iye afuna kumusocheretsa, Iye amachititsa mtima wake kukhala opapatizika ndi ovutika ngati kuti akukwera kumwamba. Mmenemo ndi mmene Mulungu amaikira mkwiyo pa anthu osakhulupirira.

[126.] Iyi ndi njira ya Ambuye wako, yoyenera. Ife tafotokoza chivumbulutso kwa anthu oganizira. [127.] Kwa iwo kudzakhala nyumba ya mtendere imene ili ndi Ambuye wawo. Iye adzakhala Mtetezi wawo chifukwa cha zimene anali kuchita. [128.] Ndipo patsiku limene adzawasonkhanitsa onse, ndi kuti: "Oh inu gulu la majini! Inu mudali kusokeletsa anthu mu unyinji wawo." Ndipo anzawo ochokera m'gulu la anthu adzati: "Ambuye ife tidapindula kuchokera kwa wina ndi mnzake, koma tsopano tafika pa mapeto ya nthawi yathu imene mudatikhazikitsira ife." Mulungu adzati: "Kumoto ndiko kumalo kwanu ndipo kumeneko mukakhala mpaka kalekale kufikira pamene Mulungu adzafuna." Ndithudi Ambuye wako ndi Wanzeru ndi Wozindikira.

[129.] Ndipo motero ndi mmene timapangira anthu olakwa

kuthandizana wina ndi mzake chifukwa cha zimene anali
kuchita. 130. Inu gulu la majini ndi anthu! “Kodi sikudadze
kwa inu Atumwi a mtundu wanu amene adali kukuuzani
za zizindikiro zanga ndi kuchenjeza za kukumana kwa
tsiku lanuli?” Iwo adzayankha, “Ife tidzichitira umboni
wodzitsutsa tokha.” Ndi moyo wa dziko lino lapansi umene
udawanyenga. Ndipo iwo adzadzichitira umboni okha kuti
iwo adali osakhulupirira. 131. Ichi ndi chifukwa chakuti
Ambuye wako samaononga Mizinda chifukwa cha zochita
zawo, pamene anthu ake sadali kudziwa. 132. Kwa aliyense
kudzaperekedwa gawo molingana ndi zimene adachita.
Sikuti Ambuye wako sadziwa zimene iwo achita.

133. Ambuye wako ndi Wolemera ndiponso ndi Wachisoni
ndipo ngati Iye afuna, akhoza kukuonongani ndi kuika
m’malo mwanu ena amene Iye wafuna monga momwe
Iye adakulengerani inu kuchokera ku mbeu ya anthu ena.
134. Ndithudi chimene inu mukulonjezedwa chidzachitika
ndipo inu simungachizembe ayi. 135. Nena, “Oh anthu anga!
Chitani chimene mungachite, ndithudi, nanenso ndili
kuchita chimene ndimachita ndipo inu mudzadziwa kuti
ndani wa ife amene adzakhala ndi mapeto abwino m’moyo
umene uli nkudza. Ndithudi anthu olakwa sadzapambana.”
136. Ndipo iwo amaika pa mbali gawo la mbewu ndi gawo
la ziweto kuti ndi za Mulungu ndipo amati: “Izi ndi za
Mulungu pamene izi ndi za mafano athu.” Koma gawo
limene amati ndi la mafano awo silifika kwa Mulungu ayi
pamene gawo la Mulungu limafika lonse kwa mafano awo!
Chiweruzo chawo ndi choipa kwambiri.

137. Motero kwa anthu opembedza mafano, mafano
awo adapangitsa kupha ana awo kukhala chinthu

chokondweretsa ndi cholinga chakuti awawononge iwo ndi kuwasokonezera chipembedzo chawo. Koma ngati Mulungu akadafuna, iwo sakadachita choncho. Motero asiyeni okha ndi zimene akupeka. 138. Potsatira zofuna zawo, iwo amati: "Nyama izi ndiponso mbewu izi ndi zoletsedwa ndipo palibe munthu amene adye kupatula okhawo amene tawaloleza." Ndipo pali nyama zina zimene amaletsa anthu kuti asakwere kapena kugwira ntchito, ndi zina zimene satchulapo dzina la Mulungu komwe ndi kumunamizira Iye. Mulungu adzawalipira chifukwa cha mabodza awo amene amapeka.

139. Ndipo iwo amati: "Zam'kati zanyamazi ndi zololedwa kudyedwa ndi anthu athu amuna okha ndipo ndi zoletsedwa kwa anthu a akazi koma ngati izo zibadwa zakufa onse amagawana. Mulungu adzawalanga chifukwa cha zonse zimene amamunamizira Iye. Ndithudi Iye ndi Wanzeru ndi Wodziwa." 140. Ndithudi olephera ndi amene, adapha ana awo mwaumbuli ndipo adaletsa zinthu zimene Mulungu adawapatsa iwo ndi kupeka bodza lokhudza Mulungu. Ndithudi iwo asokera ndipo siotsogozedwa. 141. Iye ndiye amene amapanga minda ya mbewu za mitundumitundu; zoyanga ndi zosayanga, mitengo ya tende ndi mbeu zosiyanasiyana kukoma kwake, azitona ndi chimanga cha chizungu zofanana ndi zosiyana. Idyani zipatso zake pamene zibereka ndipo perekani chaulere chake nthawi yake. Koma musawononge ayi. Ndithudi Mulungu sakonda anthu owononga.

142. Ndipo pakati pa nyama, pali zina zonyamula katundu ndi zina zosanyamula katundu. Idyani zimene Mulungu wakupatsani ndipo musatsatire mapazi a Satana ayi.

Ndithudi iye ndi mdani wooneka. 143. Tengani ng’ombe
zisanu ndi zitatu, ndi nkhosa ziwiri, ndi mbuzi ziwiri. Nena,
“Kodi Iye adaletsa zazimuna ziwiri kapena zazikazi ziwiri
kapena ana amene ali m’mimba? Ndiyankheni mozindikira
ngati mukunena zoona.”
144. Ndipo kuchokera ku ngamira, ziwiri ndi ng’ombe
ziwiri. Nena, “Kodi Iye adaletsa zazimuna ziwiri kapena
zazikazi ziwiri kapena ana amene ali m’mimba mwawo?
Kodi mudalipo pamene Mulungu adakupatsani malamulo
awa? Kodi wolakwa kwambiri ndani kuposa munthu amene
amapeka bodza lokhudza Mulungu ndi kusocheretsa anthu
popanda kuzindikira? Ndithudi Mulungu satsogolera
anthu ochita zoipa.” 145. Nena, “Ine sindipeza china
chilichonse mu zimene zavumbulutsidwa kwa ine choletsa
aliyense kudya chakudya china chilichonse kupatula
nyama yofa yokha kapena liwende kapena nyama ya
nkhumba, chifukwa zimenezo ndi zauve ndi zodetsedwa
kapena nyama ina iliyonse imene yaphedwa osati mu dzina
la Mulungu. Koma aliyense amene waumirizidwa kudya
chilichonse cha izi, osati mokondweretsedwa kapena ndi
cholinga chofuna kuswa malamulo, ndithudi, Ambuye
wako ndi wokhululukira ndi wachisoni chosatha.” 146. Ife
tidawaletsa Ayuda kudya nyama zonse zosabsyukula ndipo
tinawaletsa mafuta a ng’ombe ndi a nkhosa kupatula amene
ali pa msana ndi m’matumbo kapena amene adasakanizika
ndi mafupa. Motero tidawapatsa chilango chifukwa cha
kulakwa kwawo. Ndithudi Ife tili kunena zoonadi.
147. Ngati iwo akukunamizani, nena, “Ambuye wanu
ndi Mwini chifundo chosatha koma mkwiyo wake
siungachotsedwe pa anthu ochita zoipa.” 148. Anthu

opembedza mafano adzati: “Mulungu akadafuna, ife kapena makolo athu, sitikadatumikira milungu ina yoonjezera pa Iye ndipo ife sitikadaletsa china chilichonse.” Mmenemu ndi mmene anthu amene adalipo kale adanamira mpaka pamene analawa mkwiyo wathu. Nena, “Kodi inu muli ndi umboni uliwonse umene mungatisonyeze Ife?” Ndithudi inu simutsatira china koma zinthu zongoganiza ndiponso simuchita china chilichonse koma bodza basi.

149. Nena, “Ndi Mulungu yekha amene ali ndi umboni weniweni ndipo Iye akadafuna akadakutsogolerani nonse.” 150. Nena, “Bweretsani mboni zanu zonse zimene zikhoza kuchitira umboni kuti Mulungu adakuletsani izi. Ngati iwo apereka umboni, iwe usapereke umboni wako. Ndipo usatsatire zilakolako za iwo amene amati chivumbulutso chathu ndi chabodza, amene sakhulupirira za m'moyo umene uli nkudza ndipo amapanga milungu ina kukhala yofanana ndi Ambuye wawo.” 151. Nena, “Bwerani! Ine ndikuwerengerani zimene Ambuye wanu wakulamulani inu kuti musachite. Musapembedze milungu ina yowonjezera pa Iye; Muzionetsa chifundo kwa makolo anu; musaphe ana anu chifukwa chaumphawi, Ife timakudyetsani inu pamodzi ndi iwo; musayandikire zinthu zoipa zimene zili zoonekera kapena zili zobisika ndipo musaphe munthu amene Mulungu waletsa pokhapokha ngati pali chifukwa choyenera.” Ichi wakulamulani inu kuti muzindikire.

152. “Ndipo musayandikire chuma cha ana a masiye kupatula m'njira yabwino yowakonzera tsogolo lawo mpaka pamene iwo akula msinkhu. Kwaniritsani muyeso woyenera ndipo muyese mwachilungamo. Ife sitinyamulitsa munthu wina aliyense katundu wolemera

amene iye sangathe kunyamula. Ndipo mukamalankhula,
muzilankhula mwachilungamo ngakhale kuti nkhanizo
zikhudza abale anu ndipo kwaniritsani malonjezo a
Mulungu. Ichi wakulamurani inu kuti mudzikumbukira.”
153. Ndithu iyi ndi njira yanga yoyenera motero
itsatireni ndipo musatsatire njira zina zake chifukwa
izo zidzakusocheretsani inu ku njira yake. Ichi Iye
wakulamulani kuti mukhale angwiro. 154. Ndipo Ife
tidamupatsa Mose Buku, kumaliza ubwino wathu kwa
aliyense wochita zabwino ndiponso lofotokoza chinthu
chilichonse, ulangizi ndi chisomo kuti akhulupirire
mukukumana kwawo ndi Ambuye wawo.
155. Ili ndi Buku lodalitsika limene talivumbulutsa,
motero opani Mulungu kuti mulandire chisomo. 156. Kuti
inu musadzanene kuti: “Buku lidangovumbulutsidwa
ku magulu awiri pambuyo pathu, ndipo ife sitidadziwe
zimene adali kuwerenga.” 157. Kapena mukhoza kudzanena
kuti: “Buku la Mulungu likanavumbulutsidwa kwa ife,
ndithudi, tikadalangizidwa bwino kuposa iwo.” Ndithudi
chizindikiro chosakaikitsa chadza tsopano kuchokera
kwa a Ambuye wanu; chilangizo ndi madalitso. Kodi
wolakwa kwambiri ndani kuposa munthu amene akana
chivumbulutso cha Mulungu ndipo safuna kuchitsatira? Ife
tidzawalipira onse amene amakana zizindikiro zathu ndi
chilango chowawa chifukwa chokana kwawo. 158. Kodi iwo
ali kudikira wina kupatula angelo kuti adze kwa iwo kapena
kuti Ambuye wako adze kapena zina mwa zizindikiro za
Ambuye wako zidze? Tsiku limene zina mwa zizindikiro za
Ambuye wako zidzadza, chikhulupiriro sichidzathandiza
mzimu umene unalibe chikhulupiriro kale kapena

umene siudagwiritse ntchito bwino chikhulupiriro. Nena, “Dikirani! Nafenso tili kudikira.” 159. Ndithudi iwo amene apatukana m’chipembedzo ndi kupanga mipingo yosiyanasiyana, iwe sizikukhudza zimenezo. Nkhani yawo adzathetsa ndi Mulungu ndipo Iye adzawauza zomwe amachita.

160. Aliyense amene amachita ntchito yabwino adzalipidwa magawo khumi olingana ndi iyo ndipo aliyense amene amachita zoipa adzalandira choipa chomwecho ndipo iwo sadzaponderezedwa ayi. 161. Nena, “Ndithudi Ambuye wanga wanditsogolera ine ku njira yoyenera, ku chipembedzo changwiro, chikhulupiriro cha Abrahamu wangwiro chifukwa Abrahamu sadali mmodzi wa anthu opembedza mafano.”

162. Nena, “Ndithudi mapemphero anga, nsembe yanga, moyo wanga ndi imfa yanga zonse zili m’manja mwa Mulungu Ambuye wazolengedwa zonse.” 163. Iye alibe wothandizana naye. Pa izi ine ndalamulidwa ndipo ine ndine woyamba wa iwo ogonjera malamulo a Mulungu. 164. Nena, “Kodi ine ndifune Ambuye wina osati Mulungu pamene Iye ndi Ambuye wa zinthu zonse? Munthu aliyense adzakolola zipatso za ntchito yake ndipo palibe mzimu umene udzanyamula katundu wa wina wake. Pomaliza nonse mudzabwerera kwa Ambuye wanu; ndipo Iye adzakuuzani zomwe munali kutsutsana.” 165. Ndipo ndiye amene anakulengani kukhala mibadwo yodza pambuyo pa mibadwo yina, kulowa m’malo mwa uzake padziko lapansi. Ndipo anakukwezani m’maudindo, ena kuposa anzawo kuti akhoza kukuyesani ndi zimene wakupatsani. Ndithudi

Ambuye wanu ndi wachangu polanga koma ndithudi Iye amakhululuka, Mwini chisoni chosatha.

SURA 7 • AL-A‘RÂF

# AL A'RAF

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. *Alif Lam Mim Sad.*

2. Buku ili lavumbulutsidwa kwa iwe, mtima wako usavutike
ndi kuti uchenjeze ndi ilo ndipo ndi chikumbutso kwa
anthu okhulupirira. 3. Tsatirani zonse zimene zadza kwa
inu kuchokera kwa Ambuye wanu ndipo musatsatire wina
powonjezera pa Iye. Ndi zochepa zimene mumakumbukira!
4. Ndipo mizinda ndi yambiri imene Ife tidaononga!
Chilango chathu chidadza pa iwo usiku kapena pamene iwo
adali kugona nthawi ya masana. 5. Iwo sadalire mwa mtundu
wina uli wonse pamene chilango chathu chinadza kupatula
kuti: "Ndithudi ife tidali anthu olakwa." 6. Ndithudi Ife
tidzawafunsa onse amene uthenga wathu udatumizidwa
ndipo, ndithudi, Ife tidzafunsa Atumwi. 7. Ndipo, ndithudi,
tidzawauza modziwa ndipo, ndithudi, sikuti Ife padalibe.
8. Pa tsiku limenelo muyeso udzakhala wachilungamo.
Motero iwo amene muyeso wawo udzakhala wolemera
amenewo adzakhala opambana. 9. Koma iwo amene
muyeso wawo udzakhala wopepuka amenewo ndi olephera
chifukwa ankakana chivumbulutso chathu.

10. Ndipo Ife tidakupatsani ulamuliro padziko ndipo

tidakuikirani zofunikira mu moyo wanu koma kuthokoza
kwanu ndi kochepa. 11. Ndithudi ife tidakulengani inu
ndipo tidakupatsani maonekedwe ndipo Ife tidati kwa
angelo: "Mugwadireni Adamu" ndipo onse adamugwadira
iye kupatula Iblis amene adakana kukhala mmodzi mwa
ogwada. 12. Mulungu adati: "Kodi chakuletsa ndi chiyani
kuti umugwadire iye pamene Ine nditakulamula kutero?"
Iye adati: "Ine ndine wolemekezeka kuposa Adamu.
Inu mudandilenga ine kuchokera ku moto pamene iye
mudamulenga kuchokera ku dothi." 13. Mulungu adati:
"Choka kumene kuno. Ano simalo okhalako munthu
wa mtudzu ayi. Choka! Chifukwa iwe ndiwe mmodzi
wa anthu onyozedwa." 14. Satana adati, "Mundisunge
mpaka pa tsiku la kuuka kwa akufa." 15. Mulungu adati,
"Iwe ndiwe mmodzi wa iwo amene apatsidwa nthawi."
16. Satana adati: "Chifukwa chakuti Inu mwandisocheretsa,
ine ndidzawadikira pa njira yanu yoyenera." 17. "Ndipo
ine ndidzabuka patsogolo ndi pambuyo pawo ndipo
kuchokera ku mbali ya dzanja lamanja ndi mbali ya dzanja
lamanzere ndipo Inu simudzawapeza ambiri a iwo ali
othokoza." 18. Mulungu adati: "Tuluka muno wonyozedwa
ndi wothamangitsidwa. Ndipo aliyense amene adzakutsata
iwe ndithudi ndidzadzadza Gahena ndi inu nonse."

19. "O iwe Adamu! Khala iwe ndi mkazi wako ku
Paradiso ndipo idyani mmenemo monga mungafunire,
koma inu musadzayandikire mtengo uwu chifukwa nonse
mungadzakhale odzipondereza nokha." 20. Ndipo Satana
anawanong'oneza iwo onse ndi cholinga choti chionekere
kwa iwo chimene chinali chobisika ndi chochititsa
manyazi ndipo Satana adati: "Ambuye wanu adakuletsani

kuti musayandikire mtengo uwu chifukwa sadafune kuti
mukhale angelo kapena anthu a muyaya.” 21. Ndipo iye
adalumbira pali Mulungu nati: “Ndithudi ine ndi mmodzi
wa iwo amene amakufunirani inu zabwino.”
22. Motero iye adawanyenga iwo. Ndipo pamene iwo
adalawa mtengo uja, maliseche awo adaonekera poyera
ndipo onse anayamba kuvala masamba a ku Paradiso. Ndipo
Ambuye wawo adawaitana nati: “Kodi Ine sindidakuletseni
mtengo uwu ndiponso kukuuzani kuti: ‘Ndithudi Satana
ndi mdani wanu weniweni?” 23. Iwo adati: “Ambuye
wathu! Ife tachimwa tokha. Ngati Inu simutikhululukira
ndikutimvera chisoni, ndithudi ife tidzakhala m’gulu la
anthu olephera. 24. Iye adati: “Tsikani pansi, aliyense wa inu
adzakhala mdani wa mnzake. Padziko lapansi padzakhala
malo anu okhala ndi a chisangalalo cha kanthawi kochepa.”
25. Iye anati, “Kumeneko mudzakhala ndi moyo, kumeneko
mudzafa ndipo kuchokera kumeneko mudzaukitsidwa.”
26. Oh inu ana a Adamu! Ife takupatsani zovala kuti
mubise umaliseche wanu ndi zovala zokukongoletsani
ndi chobvala cha chilungamo chimene chili chabwino.
Zimenezo ndi zina mwa zizindikiro za Mulungu kuti akhale
okumbuka. 27. Oh inu ana a Adamu! Musalole Satana kuti
akunyengeni inu monga momwe anawatulutsitsa makolo
anu ku Paradiso, kuwavula nsalu zawo ndi kuwaonetsa
maliseche awo. Ndithudi iye pamodzi ndi gulu lake,
amakuonani inu kuchokera kumalo amene inu simungathe
kuwaona. Ndithudi Ife tidawapanga a Satana kukhala
othandiza anthu osakhulupirira.
28. Ndipo pamene iwo achita chinthu chochititsa
manyazi amati: “Tinapeza makolo athu ali kuchita

ndipo Mulungu watilamula ife kutero." Nena: "Iyayi;
Mulungu salamula chinthu chimene chili chonyansa.
Kodi inu muli kunena za Mulungu zimene simuzidziwa?"
29. Nena, "Ambuye wanga walamula chilungamo ndi kuti
muzimupembedza Iye yekha. Mpembedzeni Iye. Monga
momwe adakulengerani poyamba kwa Iye mudzabwerera."
30. Gulu lina adalitsogolera ndipo gulu lina liyenera
kusochera chifukwa, ndithudi, iwo adasankha a Satana kuti
akhale owathandiza ndi atetezi awo m'malo mwa Mulungu
ndipo anali kuganizira kuti adali otsogolera.
31. Oh inu ana a Adamu! Valani moyenera pamene muli
kupemphera ndi kuzungulira Kaaba, idyani ndi kumwa
koma musapyole muyeso ayi. Iye sakonda anthu owononga.
32. Nena, "Kodi ndani adaletsa kuvala zovala zoyenera
zimene Mulungu adapatsa akapolo ake ndiponso zakudya
zabwino?" Nena, "Zimenezo ndi zololedwa kwa anthu
okhulupirira Mulungu pa moyo uno, ndipo zidzakhala zawo
zokha pa tsiku la kuuka kwa akufa." Mmenemo ndi mmene
timaululira poyera chivumbulutso chathu kwa anthu
ozindikira. 33. Nena, "Ambuye wanga adaletsa ntchito zonse
zonyansa kaya zooneka poyera kapena zobisika, machimo,
kuponderezana popanda chilungamo, kumphatikiza
Mulungu ndi zimene sadalamulire ndi kunena za Mulungu
zimene inu simuli kuzidziwa."
34. Mtundu uliwonse uli ndi nthawi yake ya chiweruzo,
ndipo ngati nthawi yawo ikwana, iwo sangachedwetse
kapena kuonjezera ola limodzi. 35. Oh inu ana a Adamu!
Ngati Atumwi a mtundu wanu adzadza kwa inu
kudzakulalikirani chivumbulutso changa ndipo aliyense
amene akhala olungama ndi kumachita zabwino, iwo

sadzaopa china chilichonse kapena kuda nkhawa.
36. Ndipo onse amene akana chivumbulutso chathu ndi
kuchinyoza, iwo adzakhala eni ake a ku moto ndipo
adzakhala kumeneko mpaka kalekale. 37. Kodi wochimwa
kwambiri ndani kuposa munthu amene amapeka bodza
lokhudza Mulungu kapena amene akana chivumbulutso
chake? Anthu otere adzalandira gawo lawo lokonzedwera
iwo kuchokera m'Buku mpaka pamene angelo adzadza
kudzachotsa miyoyo yawo ndipo iwo adzawauza kuti,
"Kodi mafano anu aja ali kuti tsopano, amene mudali
kuwapembedza yowonjezera pa Mulungu?" Iwo adzati:
"Atithawira." Ndipo iwo adzadzichitira umboni okha kuti
iwo adali anthu osakhulupirira.
38. Mulungu adzati: "Lowani, mgulu la mitundu amene
adalipo inu musanadze, anthu ndi majin, kupita ku moto,
ndipo pamene uzidzalowa mtundu uliwonse udzakhala
uli kutemberera mtundu umene udalipo iwo usanadze
mpaka pamene adzasonkhanitsidwa onse m'moto ndipo
mtundu womaliza udzati kwa mtundu woyambirira,
'Ambuye wathu! Awa ndiwo anthu amene adatisokoneza ife
motero apatseni chilango choonjezedwa kawiri m'moto."
Iye adzati: "Kwa aliyense kuli chilango chowilikiza koma
inu simudziwa." 39. Ndipo m'badwo woyamba udzati kwa
m'badwo womaliza, "Inu simunachite zabwino kuposa ife
motero lawani chilango cha ntchito zanu zimene mudali
kuchita."
40. Ndithudi amene amati zizindikiro zathu ndi
zabodza ndipo amazinyoza izo, makomo a kumwamba
sadzatsegulidwa kwa iwo ndipo iwo sadzalowa ku Paradiso
pokhapokha ngati ngamira italowa pa diso la zingano.

Mmenemo ndi mmene timalipirira anthu ochita zoipa
malipiro awo. 41. Wawo adzakhala kama wa moto ndipo
pamwamba pawo padzakhala malawi a moto. M'menemo
ndi m'mene tidzawalipirira anthu ochita zoipa. 42. Koma
iwo amene anakhulupirira ndipo amachita ntchito
zabwino; Ife sitisenzetsa munthu katundu amene sangathe
kumunyamula; iwo ndi anthu a ku Paradiso. Ndipo
adzakhalako mpaka kalekale. 43. Ndipo Ife tidzachotsa
chidani m'mitima mwawo ndipo mitsinje idzayenda
pansi pa mapazi awo ndipo iwo adzati: "Kuyamikidwa
ndi kwa Mulungu amene watitsogolera ife ku izi ndipo
ife sitikadakhala otsogozedwa pakadapanda Mulungu
kutitsogolera! Ndithudi Atumwi a Ambuye wathu adadza
ndi choonadi." Ndipo zidzanenedwa kwa iwo kuti: "Iyi
ndiyo Paradiso imene mwailandira chifukwa cha ntchito
zanu zimene mudali kuchita."

44. Ndipo anthu okhala ku Paradiso adzaitana anthu a
ku Moto. "Ndithudi chimene adatilonjeza ife Ambuye
wathu tachipeza kuti ndi choona. Kodi inu mwapeza
chomwe adakulonjezani Ambuye wanu kuti ndi choona?"
Iwo adzati: Inde. Ndipo wofuula adzanena pakati pawo:
"Matemberero a Mulungu ali pa anthu olakwa." 45. Iwo
amene anali kuletsa anzawo kutsatira njira ya Mulungu
ndipo amafuna kuti iyo ikhale yokhotakhota ndipo adalibe
chikhulupiriro m'moyo umene uli nkudza.

46. Ndipo pakati pawo padzakhala chotchinga ndi
chipupa mmene mudzakhala anthu amene adzazindikira
wina aliyense poona zizindikiro zawo. Iwo adzaitana
anthu a ku Paradiso: Mtendere ukhale pa inu. Koma
panthawi imeneyo iwo adzakhala asadalowe ku Paradiso

koma iwo adzakhala ndi chikhulupiriro choti adzalowanso
mopanda chikaiko. 47. Ndipo pamene iwo adzaona iwo
amene adzakhala ku moto, iwo adzati: “Oh Ambuye
wathu! Musatiike ife malo a anthu oipa.” 48. Ndipo anthu
a m’chipupa adzawaitana anthu omwe adzawadziwa
ndi zizindikiro zawo ndipo adzati: “Kodi kuchuluka
kwanu, kwakuthandizani chiani ndiponso mwano umene
mumaonetsa ku chipembedzo?” 49. Kodi awa ndi anthu
amene munkalumbira kuti sadzalandira chisomo cha
Mulungu? “Lowani ku Paradiso, inu simudzachita mantha
ndiponso simudzada nkhawa ayi.”
50. Ndipo anthu a ku Moto adzaitana anthu a ku Paradiso
kuti, “Tithireni madzi kapena china chilichonse chimene
Mulungu wakupatsani inu!” Anthu a ku Paradiso adzati,
“Mulungu adaletsa zonse ziwiri kuti anthu osakhulupirira
alandire.” 51. “Iwo amene adasandutsa chipembedzo chawo
ngati nthabwala ndi choseweretsa ndipo adali kunyengedwa
ndi zokoma za m’moyo wa padziko lapansi. Motero lero
Ife tiwaiwala monga mmene adaiwalira za kukumana kwa
tsiku lawoli ndi chifukwa chokana zizindikiro zathu.”
52. Ndithudi Ife tawabweretsera Buku m’mene talongosola
za nzeru, chilangizo ndi madalitso kwa anthu okhulupirira
kwenikweni. 53. Kodi iwo akudikira kuti chikwaniritsidwe?
Patsiku limene chidzakwaniritsidwe iwo amene adaliiwala
kale adzati, “Ndithudi, Atumwi a Ambuye wathu adadza ndi
choonadi. Kodi palibe wina amene akhoza kutilankhulira
m’malo mwathu? Kapena kuti tibwezedwe kupitanso ku
dziko lapansi kuti tikachite nthito zabwino osati zoipa
zimene timachita?” Ndithudi iwo adadziononga okha
ndipo chonse chimene adali kupeka chawathawira iwo.

54. Ndithudi Ambuye wanu ndi Mulungu, amene
m'masiku asanu ndi limodzi adalenga kumwamba ndi dziko
lapansi ndipo atatero adabuka pamwamba pa Mpando
wake wa Chifumu. Iye amavundikira usiku ndi usana
ndipo mofulumira usiku umatsata usana. Ndipo dzuwa,
mwezi ndi nyenyezi zimayenda motsatira malamulo
ake. Ndithudi zake ndi zolengedwa zonse ndi ulamuliro.
Olemekezeka akhale Mulungu, Ambuye wa zolengedwa
zonse. 55. Pemphani kwa Ambuye wanu modzichepetsa ndi
mwamseri. Iye sakonda anthu oswa malamulo. 56. Ndipo
musayambitse chisokonezo padziko ilo litakonzedwa
ndipo pemphani kwa Iye mwamantha ndi chikhulupiriro;
ndithudi, chifundo cha Mulungu chili pafupi ndi anthu
ochita zabwino.

57. Iye ndi amene amatumiza mphepo ngati yobweretsa
uthenga wabwino umene umadza pambuyo pa chisomo
chake. Mpaka pamene iyo isonkhanitsa mitambo yolemera,
timaiyendetsa kupita ku nthaka yakufa ndipo timatumiza
mvula kuti igwe pa iyo. Ndipo timameretsa zipatso za
mitundu mitundu. Mmenemu ndi mmene tidzadzutsire
anthu akufa kuti mwina mukhoza ku chenjezedwa.
58. Nthaka yabwino imabereka zipatso mwachifuniro cha
Mulungu. Nthaka yoipa siibereka chilichonse pokhapokha
movutikira. Motero timafotokoza zivumbulutso zathu
poyera kwa anthu amene amathokoza.

59. Ndithudi Ife tidatumiza Nowa kwa anthu ake ndipo iye
adati: "Oh anthu anga! Pembedzani Mulungu! Inu mulibe
mulungu wina kupatula Iye yekha. Ndithudi ine ndili
kuchita mantha ndi chilango chowawa chimene chidzadza
pa inu patsiku lalikulu." 60. Atsogoleri a anthu ake adati:

“Ndithudi ife tili kuona kuti iwe wasochera kwambiri.”
61. Iye adati: “Oh anthu anga! Ine sindine wosochera, koma
ndine Mtumwi wochokera kwa Ambuye wazolengedwa
zonse.” 62. “Ndipo ndili kukulalikirani uthenga wa Ambuye
wanga ndi kukulangizani inu. Ndipo ndili kudziwa
kuchokera kwa Mulungu zimene inu simukudziwa ayi.”
63. “Kodi inu mukudabwa kuti kwadza kwa inu chenjezo
lochokera kwa Ambuye wanu kudzera mwa munthu amene
ali pakati panu kuti akuchenjezeni kuti mukhale anthu
oopa Mulungu ndi kuti mupeze chisomo chake?” 64. Koma
iwo adamutsutsa ndipo Ife tidamupulumutsa iye pamodzi
ndi amene adali ndi iye M’chombo ndipo tidawamiza onse
amene adakana chivumbulutso chathu. Ndithudi iwo adali
anthu akhungu.

65. Ndipo kwa Ad tidatumiza m’bale wawo Hud. Iye
adati: “Oh anthu anga! Pembedzani Mulungu! Inu mulibe
mulungu wina koma Iye yekha basi. Kodi simuopa?”
66. Atsogoleri a anthu osakhulupirira ochokera ku mtundu
wa Hud adati: “Ife tili kukuona kuti iwe ndiwe wopusa ndipo
ife tili kuganiza kuti ndiwe mmodzi wa anthu a bodza.”
67. Iye adati: “Oh anthu anga! Ine sindine wopusa koma
ndine Mtumwi wochokera kwa Ambuye wazolengedwa
zonse.” 68. “Ine ndili kukulalikirani Uthenga wa Ambuye
wanga ndipo ndine mchenjezi wanu wokhulupirika.”
69. “Kodi mukudabwa kuti kwadza chikumbutso chochokera
kwa Ambuye kudzera mwa munthu wa mtundu wanu
kuti akhale okuchenjezani inu? Ndipo kumbukirani kuti
adakupangani inu kukhala alowam’malo a anthu a Nowa
ndipo adakuonjezerani mphamvu pachilengedwe. Motero
kumbukirani madalitso a Mulungu kuti mupambane.”

70. Iwo adati: "Iwe wadza kuti ife tizingopembedza
Mulungu yekha ndi kusiya milungu imene makolo athu
adali kupembedza. Motero bweretsa chimene ukutiopseza
nacho ngati zimene uli kunena ndi zoona." 71. Iye adati:
"Mkwiyo wa Ambuye wanu ndiponso chilango chake
chadza kale pa inu. Kodi inu mukutsutsana ndi ine pa
mayina amene inu ndi makolo anu mudapeka, opanda
chilolezo cha Mulungu? Dikirani nanenso ndili mmodzi
mwa odikira." 72. Ife tidamupulumutsa iye ndi onse amene
adali naye mwa chifundo chathu ndipo tidadula maziko ya
onse amene anatsutsa chivumbulutso chathu ndipo iwo
adali osakhulupirira.
73. Ndipo kwa anthu a Thamud, Ife tidawatumizira
m'bale wawo Saleh. Iye adati: "Oh anthu anga! Pembedzani
Mulungu. Inu mulibe mulungu wina koma Iye yekha.
Ndithudi wadza umboni wokhulupirika kuchokera kwa
Ambuye wanu. Iyi ndi Ngamira yaikazi ya Mulungu,
chizindikiro kwa inu. Motero ilekeni kuti izidya m'dziko
la Mulungu ndipo musaizunze ayi chifukwa mungapute
chilango chowawa." 74. "Ndipo kumbukirani pamene
Iye adakupangani inu kuti mukhale alowa m'malo a
Ad, ndipo adakupatsani malo okhala m'dziko lino. Inu
mwamanga nyumba zolemekezeka m'chidikha chake
ndiponso mwaboola nyumba pakati pa mapiri ake. Motero
kumbukirani zokoma za Mulungu ndipo musachulukitse
kuwononga padziko lapansi." 75. Atsogoleri a anthu amene
amadzikweza mu anthu ake anati kwa anthu ofoka amene
adakhulupirira mwa iwo: "Kodi mukudziwa kuti Saleh ndi
wotumidwa kuchokera kwa Ambuye wake?" Iwo adati:
"Ndithudi ife takhulupirira mzimene iye watumidwa."

76. Iwo amene adali odzikuza adati: "Ndithudi ife tili
kuzikana zonse zimene inu muli kuzikhulupirira." 77. Motero
iwo adapha ngamira yaikazi ija ndipo ananyoza lamulo la
Ambuye wawo ndipo adati: "Iwe Saleh! Bweretsa chimene
udatiopseza nacho ngati iwe ndiwe Mtumwi woona."
78. Motero nthawi yomweyo chivomerezi chidagwa pa iwo
ndipo pamene kumacha m'mawa onse adali lambilambi
m'nyumba zawo atafa. 79. Motero Saleh adachoka nati, "Oh
anthu anga! Ine, ndithudi, ndapereka uthenga wa Ambuye
wanga ndipo ndakupatsani chilangizo chabwino koma inu
simukonda anthu okuchenjezani."

80. Ndi pamene Loti adanena kwa anthu ake, "Kodi inu
mukuchita zinthu zonyansa zimene palibe mtundu wa
anthu umene udachitapo ndi kale lomwe?" 81. "Ndithudi inu
mufuna kukwaniritsa zilakolako za matupi anu ndi amuna
anzanu m'malo mwa akazi? Iyayi, ndithudi, inu ndinu
anthu ochimwa kwambiri." 82. Ndipo yankho la anthu ake
silinali lina koma adati: "Achotseni iwo mu Mzinda wanu.
Awa ndi anthu amene afuna kukhala angwiro." 83. Ndipo Ife
tidamupulumutsa iye pamodzi ndi omutsatira ake kupatula
mkazi wake amene adali mmodzi mwa otsalira m'mbuyo.
84. Ndipo tidagwetsa pa iwo mvula yambiri. Onani mapeto
a anthu ochita zoipa.

85. Kwa anthu a ku Midiyani tidatumiza m'bale wawo
Shaibu. Iye anati: "Oh anthu anga! Pembedzani Mulungu,
inu mulibe mulungu wina koma Iye yekha. Ndithudi
chizindikiro chooneka chadza kwa inu kuchokera kwa
Ambuye wanu motero perekani muyeso woyenera ndipo
yesani zonse moyenera ndipo musachite chinyengo kwa
anthu pa katundu wawo ndipo musawononge dziko lapansi

pambuyo poti layeretsedwa kale. Chimenecho ndicho
chinthu chabwino kwa inu ngati inu ndinu okhulupirira
kwenikweni." 86. "Ndipo musakhale mu msewu uliwonse
ndi kumaopseza anthu okhulupirira ndi kuwaletsa kutsatira
njira ya Mulungu ndi kufunafuna njira yoti mukhotetsere
njirayo. Kumbukirani mmene adakuchulukitsirani inu
pamene mudali ochepa. Ndipo onani mmene adalili
mapeto a anthu ochita zoipa." 87. "Ndipo ngati lilipo gulu
lina pakati panu limene lidakhulupirira mu Uthenga umene
ndidatumizidwa ndi gulu limene silidakhulupirire motero
pilira mpaka pamene Mulungu aweruza pakati pathu. Iye
ndiye wabwino mwa oweruza onse."

88. Mafumu odzikweza a gulu lina la mtundu wake adati:
"Iwe Shaibu! Ndithudi ife tidzakuthamangitsa iwe mu
mzinda wathu pamodzi ndi iwo amene akhulupirira ndi
iwe kapena kuti mubwerere ku chipembedzo chathu."
Iye adati: "Chiyani! Ngakhale kuti zikutinyansa?"
89. "Ndithudi ife timpekera Mulungu bodza ngati tibwerera
ku chipembedzo chanu pamene Mulungu watipulumutsa
ife ku icho. Ndipo ife sitikadatha mwa njira iliyonse
kubwerera ku icho pokhapokha ndi chifuniro cha Mulungu.
Ambuye wathu amadziwa chili chonse. Mwa Mulungu ife
taika chikhulupiriro chathu. Ambuye wathu! Weruzani
pakati pa ife ndi anthu athu mwachoonadi chifukwa
Inu ndinu wodziwa kuweruza." 90. Ndipo mafumu a iwo
amene sadakhulupirire a mtundu wa Shaibu adati: "Ngati
inu mutsatira Shaibu ndithudi, mudzakhala olephera pa
zochita zanu." 91. Ndipo nthawi yomweyo chivomerezi
chidagwa pa iwo ndipo onse adali lambilambi m'nyumba
zawo. 92. Onse amene adatsutsa Shaibu adakhala ngati

sadakhalenso malo amenewa. Onse amene sadakhulupirire mwa Shaibu adali otaika. 93. Motero Shaibu adawasiya iwo nati: “Oh inu anthu anga! Ndithudi ine ndidakuuzani uthenga wa Ambuye wanga ndipo ndakupatsani ulangizi wabwino. Kodi ine ndingamvere bwanji chisoni anthu osakhulupirira?”

94. Ndipo Ife sitimatumiza Mtumwi ku mzinda wina uli wonse koma timagwetsa pa anthu ake umphawi, matenda ndi matsoka kuti akhoza kudzichepetsa. 95. Ndipo tidasanduliza matsoka kukhala mwayi mpaka pamene iwo adachuluka ndikukhala ndi chuma ndipo adayamba kunena kuti: “Makolo athu nawonso adali kuona zosangalatsa ndiponso mavuto.” Ndipo Ife tidawapatsa chilango mwadzidzidzi pamene iwo sadali kudziwa. 96. Ndipo anthu a m’Mizinda imeneyi akadakhulupirira ndi kuopa uchimo, tikadawatsegulira madalitso kuchokera kumwamba ndi padziko lapansi. Koma iwo adakana choonadi. Motero Ife tidawalanga chifukwa cha zimene adali kuchita. 97. Kodi anthu a m’mizinda amaganiza kuti adali wotetezedwa ku chilango chathu ngati chikanadza kwa iwo nthawi ya usiku pamene iwo adali kugona? 98. Kapena anthu a m’Mizinda amaganiza kuti anali otetezedwa ku chilango chathu chimene chingadze kwa iwo masana pamene ali kusewera? 99. Kodi iwo amaganiza kuti ndi otetezedwa ku chiweruzo cha Mulungu? Palibe amene angaganize kuti ndiotetezedwa kuchilango cha Mulungu, kupatula anthu otayika.

100. Kodi m’badwo uno, umene wadza pambuyo pa wina, siuzindikira kuti ngati Ife titafuna, tikhoza kuulanga chifukwa cha machimo awo? Ndipo timaika chimatiro m’mitima mwawo kuti asamve. 101. Imeneyo ndi mizinda

imene nkhani zake tili kukuuza iwe. Ndithudi kudadza
kwa iwo Atumwi awo ndi zizindikiro zooneka. Koma iwo
sadakhulupirire zimene adazikana kale. Kotero Mulungu
amamata mitima ya anthu osakhulupirira. 102. Ife sitidaone
ambiri mwa iwo amene adasunga malonjezo koma Ife
tidawapeza, ndithudi, ambiri a iwo ali anthu ochita zoipa.
103. Atapita awa, Ife tidatumiza Mose ndi zizindikiro
zathu kwa Farao ndi mafumu ake koma iwo adazikana.
Motero taona mapeto a anthu ochita zoipa. 104. Ndipo
Mose adati: "Oh Farao! Ine ndine Mtumwi wochokera
kwa Ambuye wazolengedwa zonse. 105. Ndithudi ine
sindidzanena china chilichonse chokhudza Mulungu
kupatula choonadi. Ndithudi ine ndakubweretserani
chizindikiro chosakaikitsa kuchokera kwa Ambuye wanu.
Motero alole ana a Israyeli kuti apite ndi ine." 106. Farao
adati: "Ngati wabwera ndi chizindikiro, chionetse msanga
ngati uli kunena zoona." 107. Ndipo Mose adaponya pansi
ndodo yake ndipo nthawi yomweyo idasanduka njoka
yeniyeni. 108. Ndipo iye adatulutsa dzanja lake ndipo nthawi
yomweyo lidasanduka loyera kwa iwo amene adaliona.
109. Mafumu a anthu a Farao adati: "Ndithudi munthu
uyu ndi wodziwa matsenga kwambiri. 110. Iye akufuna
kukutulutsani inu mu dziko lanu, nanga inu mukuti
bwanji?" 111. Iwo adati: "Bamusungani pa kanthawi, iye
pamodzi ndi m'bale wake ndipo tumizani anthu ku mizinda
kuti akasonkhanitse." 112. Ndipo kuti abweretse kwa iwe
onse odziwa matsenga."
113. Ndipo anthu a matsenga adadza kwa Farao. Iwo
adati: "Ndithudi ife tidzapeza malipiro abwino ngati ife
tipambana." 114. Iye adati: "Inde ndipo inu mudzakhala

pafupi ndi ine.” 115. Iwo adati: “Oh iwe Mose! Kapena
uyambe ndiwe kuponya ndodo yako kapena tiyambe
ndife?” 116. Iye adati: “Yambani ndinu.” Ndipo pamene iwo
adaponya, iwo adalodza maso a anthu ndi kuwachititsa
mantha ndipo adaonetsa matsenga akulu. 117. Ndipo ife
tidati kwa Mose: “Tsopano ponya pansi ndodo yako.”
Ndipo nthawi yomweyo ndodo yake idameza zonse za
matsenga zimene iwo amaonetsa. 118. Motero choonadi
chidakhazikitsidwa ndipo zochita zawo zidakhala zopanda
pake. 119. Motero iwo adagonjetsedwa nthawi yomweyo
ndipo anachititsidwa manyazi. 120. Ndipo anthu a matsenga
onse adagwetsa mphumi zawo pansi ndi kulambira. 121. Iwo
adati, “Ife takhulupirira mwa Ambuye wa zolengedwa
zonse.” 122. “Ambuye wa Mose ndi Aroni.”

123. Ndipo Farao adati, “Kodi inu mwakhulupirira mwa
iye popanda chilolezo changa? Ndithudi chimenechi ndi
chiwembu chimene inu mwakonza mu mzinda ndi cholinga
chotulutsa anthu ake koma posachedwapa mudzadziwa.”
124. “Ndithudi ine ndidzadula manja anu ndi mapazi anu
mosiyanitsa ndipo ndidzakupachikani nonse.” 125. Iwo
adamuyankha: “Ndithudi ife tili kubwerera kwa Ambuye
wathu.” 126. “Ndipo inu mufuna kubwezera kwa ife chifukwa
cha kuti takhulupirira mu zizindikiro za Ambuye wathu
pamene zalangizidwa kwa ife! Ambuye wathu! Tipatseni
kupirira ndipo konzani kuti ife tife ngati Asilamu.”

127. Mafumu a anthu a Farao adati: “Kodi inu mukumusiya
Mose ndi anthu ake kuti azichita zoipa m’dziko ndi kukusiya
iwe ndi milungu yako?” Iye adayankha, “Ife tidzapha ana
awo amuna ndi kusiya ana awo akazi ndi moyo ndipo Ife
ndithudi tili ndi mphamvu pa iwo.” 128. Mose adawauza

anthu ake kuti, "Pemphani thandizo kwa Mulungu ndipo mupirire. Ndithudi Mwini wake wa dziko lino ndi Mulungu. Iye amalipereka ngati mokhalamo kwa iwo, akapolo ake, amene Iye wawasankha ndipo mapeto abwino adzakhala kwa anthu angwiro." 129. Iwo adati, "Ife tidali kuzunzidwa iwe usadadze kwa ife ndipo tikuzunzidwabe pamene iwe wadza." Iye adati: "Mwina Ambuye wanu akhoza kuwononga adani anu ndi kukupangani inu kukhala olamulira m'dziko kuti Iye aone mmene muzidzachitira."

130. Ndithudi Ife tidawalanga anthu a Farao ndi chilala cha zaka zambiri ndi kuchepa kwa zipatso kuti mwina akhoza kukumbuka. 131. Koma pamene zabwino zinali kudza kwa iwo, iwo amati: "Zimenezi ndi zotiyenera." Koma ngati choipa chimadza pa iwo, adali kunena kuti chadza chifukwa cha Mose ndi anthu ake. Dziwani! Ndithudi zoipa zawo zimachokera kwa Mulungu koma ambiri a iwo sadziwa.
132. Iwo adati: "Zodabwitsa zina zilizonse zimene ungabweretse ndi cholinga chotizunguza ife sitidzakukhulupirira ayi."

133. Motero ife tidawatumizira chigumula ndi dzombe, nsabwe, achule, ndi magazi kukhala zizindikiro zoonadi zosiyanasiyana zooneka komabe iwo adazikana izo chifukwa chakuti adali anthu ochimwa. 134. Ndipo pamene mlili unali kudza pa iwo, iwo amati: "Oh Mose! Chonde, pempha kwa Ambuye wako, m'malo mwathu, chifukwa cha lonjezo lake kwa iwe. Ngati iwe utichotsera mliliwu, ndithudi, ife tidzakhulupirira mwa iwe ndipo tidzawalola ana a Israyeli kuti apite nawe." 135. Koma pamene Ife tidachotsa mlili pa iwo mpaka nthawi yokhazikika, imene adzaifika, taona! Iwo adaphwanya lonjezo.

136. Motero ife tidawabwezera chipongwe chawo. Ndipo
tidawamiza m’nyanja chifukwa chakuti iwo adakana
zizindikiro zathu ndipo sadafune kulabadira. 137. Ndipo Ife
tidawapatsa anthu amene amati ndi ofooka ulamuliro wa
maiko a ku m’mawa ndi ku madzulo, amene tidawadalitsa.
Ndipo Mau olemekezeka Ambuye wako kwa ana a Israyeli,
adakwaniritsidwa chifukwa cha kupirira kwawo. Ndipo
Ife tidaononga zinthu zonse zomwe Farao ndi anthu ake
adapanga ndi zimene anali kumanga.

138. Ndipo Ife tidawatsogolera ana a Israyeli powoloka
nyanja ndipo iwo adapeza anthu omwe anali kupembedza
mafano awo. Iwo adati, “Mose tipangire ife mulungu
wolingana ndi milungu yawo.” Mose anayankha: “Ndithudi
inu ndinu anthu osadziwa.” 139. Ndithudi anthu awa
adzawonongeka chifukwa chopembedza mafano. Ndipo
ntchito zawo zonse ndi zopanda pake. 140. Iye anati: “Kodi
ndikufunireni mulungu wina kupatula Mulungu weniweni
pamene Iye wakulemekezani inu kuposa mitundu yonse.”
141. Ndi pamene Ife tidakupulumutsani inu kwa anthu a
Farao, amene adali kukuzunzani kwambiri, kupha ana anu
amuna ndi kusiya ana anu akazi a moyo. Ndipo mmenemo
munali mayesero akulu ochokera kwa Ambuye wanu.

142. Ife tidamusankhira Mose masiku makumi atatu ndipo
tinaonjeza masiku khumi ena, motero iye adakwaniritsa
nthawi imene adasankhidwa ndi Ambuye wake ya masiku
makumi anayi ndipo Mose anamuuza m’bale wake Aroni
kuti: Lowa m’malo mwanga pakati pa anthu anga. Uchite
zinthu za ngwiro ndipo usatsatire njira ya anthu ochita
zoipa. 143. Ndipo pamene Mose adabwera panthawi ndi
malo osankhidwa ndi Ife, Ambuye wake adalankhula naye

ndipo iye adati: "Oh Ambuye wanga! Dzionetseni inu kwa
ine kuti ndikuoneni." Mulungu adati: "Iwe siudzandiona
Ine ayi. Koma uone kuphiri ndipo ngati ilo lingakhalebe
chikhalire ndiye kuti ukhoza kundiona Ine." Ndipo pamene
Ambuye wake anadzionetsera pa phiri, phiri lidaphwanyika
ndi kusanduka fumbi lokhalokha ndipo Mose adagwa pansi
ndipo adakomoka koma pamene anatsitsimuka iye adati:
"Ulemerero ukhale kwa Inu. Ine ndalapa kwa Inu ndipo ine
ndine woyamba wa anthu okhulupirira."
144. Mulungu adati: "Oh iwe Mose! Ine ndakusankha iwe
kukhala wapamwamba pakati pa anthu a mitundu yonse
polankhula nawe. Motero gwiritsa zimene takupatsa
ndipo khala othokoza." 145. Ndipo tidamulembera iye, pa
matabwa, malamulo osiyanasiyana ndi malangizo okhudza
zinthu zonse ndipo tidati kwa iye, "Gwiritsa malamulo
awa mwamphamvu ndiponso lamulira anthu ako kuti
awatsatire bwinobwino. Ine ndidzakuonetsa midzi ya
anthu oswa malamulo." 146. Ine ndidzawabisila zizindikiro
zanga anthu a odzikweza ndi ochita zoipa mopanda
chilungamo padziko ngakhale kuti iwo ataona chizindikiro
china chilichonse, sadzachikhulupirira. Ngati aona njira
yoyenera, iwo sadzaitsata, koma akaona njira yopotoka, iwo
adzaitsatira iyo; chifukwa chakuti iwo adakana zizindikiro
zathu ndipo sadafune kuzimvera ayi. 147. Iwo amene akana
zizindikiro zathu ndi kukumana kwa patsiku la chiweruzo
ntchito zawo ndi zopanda pake. Kodi iwo amayembekeza
kuti adzalipidwa kuposa zimene amachita?
148. Ndipo anthu ake a Mose adaumba, iye atachoka,
kuchokera ku mphete ndi ndolo zawo, chifanizo cha mwana
wa ng'ombe amene adali ndi mawu. Kodi iwo sadathe kuona

kuti iyo siinathe kuwalankhula kapena kuwalondolera
njira? Iwo adaipembedza iyo, kotero adalakwa. 149. Koma
pamene iwo adazindikira ndi kuona kuti adalakwa, iwo
adati: “Ngati Ambuye wathu sakhala ndi chifundo ndi
ife ndi kutikhululukira, ndithudi, ife tidzakhala anthu
otayika.” 150. Ndipo pamene Mose adabwerera kwa anthu
ake, wokwiya ndi wachisoni, iye adati: “Kodi ndi chinthu
choipa bwanji chimene mwachita pamene ine kudalibe!
Kodi inu munafulumira ndi kusiya kupembedza Ambuye
wanu?” Ndipo iye adaponya pansi matabwa a malamulo,
nagwira mutu wa m’bale wake ndi kumukokera kwa iye.
Aroni adati: “Iwe mwana wa Amayi anga! Ndithu anthu
awa adandiposa mphamvu ndipo adakhala pang’ono
kundipha ndipo usalole kuti adani anga asangalale pa ine
ndipo usandiike pa gulu la anthu ochita zoipa.” 151. Mose
adati: “Ambuye wanga! Ndikhululukireni ine pamodzi ndi
m’bale wanga ndipo tilowetseni m’chisoni chanu chifukwa
Inu ndinu oonetsa chisoni kwambiri kuposa onse omwe
amaonetsa chisoni.”

152. Ndithudi iwo amene adapembedza ng’ombe, mkwiyo
wa Ambuye wawo ndi kupeputsidwa kudzadza kwa iwo
m’moyo uno. Mmenemo ndi mmene timalipirira anthu
opeka mabodza. 153. Koma iwo amene anachita zoipa ndipo
pambuyo pake adalapa ndi kukhala ndi chikhulupiriro,
ndithu Ambuye wako pambuyo pa izo ndi wokhululukira
ndi wachisoni chosatha.

154. Ndipo pamene mkwiyo wake udatha, Mose
adatenga matabwa a malamulo, amene m’zolembedwa
zake mudali chilangizo ndi chifundo kwa anthu amene
amaopa Ambuye wawo. 155. Ndipo Mose adasankha,

pakati pa anthu ake, amuna makumi asanu ndi awiri kuti
adzakumane nafe ndipo pamene nthaka idagwedezeka
pamapazi pawo, Mose adati: "Chikadakhala chifuniro
chanu, Ambuye, mukadawaononga iwo ndi ine kale.
Kodi inu mungationonge chifukwa cha ntchito za anthu
amene ali pakati pathu? Awa ndi mayesero anu, amene
Inu mumasocheretsa aliyense amene mwamufuna ndi
kutsogolera yemwe mwamufuna. Inu nokha ndinu Mtetezi
wathu ndipo tichitireni chisoni chifukwa Inu ndinu
wopambana onse amene amakhululukira." 156. "Ndipo
tipatseni ife zabwino m'moyo uno ndiponso m'moyo umene
uli nkudza. Ndithudi ife tabwerera kwa Inu." Mulungu
adati: "Ine ndidzaonetsa chilango changa kwa aliyense
amene ndimufuna ndipo chifundo changa chimakwanira
zinthu zonse. Ine ndidzaonetsa chisoni kwa onse amene
amalewa zoipa ndipo amapereka chaulere ndi iwo amene
amakhulupirira zizindikiro zathu." 157. Iwo amene amatsatira
Mtumwi kapena Mneneri amene sadziwa kulemba ndi
kuwerenga, amene mbiri yake inalembedwa m'Buku la
chipangano chakale ndi mu chipangano chatsopano.
Iye amawalamulira kuchita zabwino ndipo amawaletsa
kuchita zoipa. Ndipo amawaloleza zabwino ndi kuwaletsa
zonyansa. Iye amawapeputsira katundu wolemera amene
adali pa iwo. Motero iwo amene akhulupirira mwa iye ndi
kumulemekeza, ndi kumuthandiza iye ndi kutsata kuunika
kumene kwatumizidwa ndi iye, ndi okhawo amene
adzakhala opambana.

158. Nena, "Oh inu anthu! Ndithudi ine ndatumizidwa
ngati Mtumwi wa Mulungu kwa inu nonse, yemwe ali
Mwini ufumu wakumwamba ndi wa padziko lapansi.

Kulibe mulungu wina koma Iye yekha. Iye amapereka moyo ndi imfa. Motero khulupilirani mwa Mulungu ndi mwa Mtumwi wake, Mtumwi yemwe sadziwa kuwerenga ndi kulemba, amene amakhulupirira mwa Mulungu ndi m'Mawu ake. Ndipo mutsatireni iye kuti mukhale otsogozedwa." 159. Pakati pa anthu a Mose, pali anthu ena amene amatsogolera mwa choonadi ndipo anali kuchita chilungamo.

160. Ndipo Ife tidawagawa kukhala mafuko khumi ndi iwiri. Ndipo Ife tidamupatsa Mau Mose, ndipo tidati: "Menya thanthwe ndi ndodo yako." Pomwepo a kasupe khumi ndi awiri anatumphuka kuchokera m'thanthwe ndipo gulu lililonse lidadziwa chitsime chake. Ife tidawavundikira ndi mitambo ndipo tidawatumizira Manna ndi mbalame ndipo tidati: "Idyani zinthu zabwino zimene takupatsani inu." Iwo sadatilakwire Ife koma analakwira mizimu yawo. 161. Ndi pamene zidanenedwa kwa iwo: "Khalani mu Mzinda uwu ndipo idyani mmene mungafunire ndipo munene kuti: 'Tikhululukireni machimo athu; ndipo lowani pa khomo modzichepetsa.' Ife tidzakukhululukirani machimo anu. Ndipo tidzaonjezera mphotho ya iwo amene achita zabwino." 162. Koma anthu oipa amene adali pakati pawo, adasintha mawu amene adapatsidwa, motero Ife tidawatumizira chilango kuchokera kumwamba chifukwa cha kulakwa kwawo.

163. Ndipo afunse iwo za Mzinda umene udali pa mbali pa nyanja pamene iwo adaphwanya malamulo a tsiku la Sabata pamene nsomba zinali kusewera pafupi ndi kumatulutsa mitu yawo pamene sizidali kutero pa masiku ena. Motero Ife tidawayesa chifukwa iwo adali anthu oswa

malamulo. 164. Ndi pamene gulu lina lidati, "Kodi ndi
chifukwa chiyani uli kulalikira kwa anthu amene Mulungu
ali pafupi kuwaononga kapena kuwalanga kwambiri?" Iwo
adayankha kuti; "Ife tisadzakhale ndi mlandu kwa Ambuye
wanu ndiponso kuti mwina iwo angaope Mulungu."
165. Ndipo pamaso pa iwo amene adaiwala chikumbutso
chimene chidaperekedwa kwa iwo, Ife tidapulumutsa iwo
amene amaletsa zoipa ndipo Ife tidawalanga amene adali
olakwa ndi chilango chowawa chifukwa cha machimo awo.
166. Ndipo pa nthawi imene iwo adapitiriza kuchita zinthu
zimene adaletsedwa kuchita, Ife tidati kwa iwo! "Khalani
anyani, onyozeka ndi okanidwa."
167. Ndi pamene Ambuye wako adalamula kuti
adzawatumizira, mpaka tsiku la chiweruzo, iwo amene
azibweretsa mazunzo ndi mnyozo pa iwo. Ndithudi
Ambuye wako ndi wachangu polanga. Ndipo, ndithudi,
Iye ndi wokhululukira ndipo ndi Wachisoni chosatha.
168. Ife tidawamwaza pa dziko lapansi m'magulu
osiyanasiyana. Ena adali anthu angwiro pamene ena ndi
anthu oipa. Ndipo Ife tidawayesa powapatsa madalitso ndi
matsoka kuti mwina akhoza kubwerera.
169. Ndipo lidalowa m'malo gulu lina loipa limene
linatenga Buku, koma iwo adasankha zinthu zopanda pake
za pa dziko lapansi. Ndipo iwo adati "Tidzakhululukidwa."
Koma zitawapezanso zinthu zopanda pake za mtundu
womwewo iwo akadazilandira. Kodi lonjezo la m'Buku
silinalandiridwe kuchokera kwa iwo kuti sadzanena chili
chonse chokhudza Mulungu kupatula choonadi? Ndipo
iwo aphunzira zomwe zili m'menemo. Ndipo dziko limene
lili nkudza ndi labwino kwa anthu oopa Mulungu. Kodi inu

mulibe nzeru? 170. Akakhala iwo amene amatsatira moona
Mau a Mulungu ndi kupitiriza mapemphero, ndithudi, Ife
sitidzaononga mphotho za anthu ochita ntchito zabwino.
171. Ndi pamene tidakweza phiri ndikuliika pamwamba
pawo kukhala ngati mthunzi ndipo iwo amaganiza
kuti liwagwera. Ndipo Ife tidati, "Gwiritsani chimene
takupatsani inu ndipo kumbukirani zimene zili m'kati
mwake kuti mukhale oopa Mulungu ndi kumumvera Iye."

172. Ndi pamene Ambuye wako adabweretsa kuchokera
kwa ana a Adamu, kuchokera m'misana mwawo mbeu yawo
ndipo adawapanga kuti alumbire okha. Iye adati, "Kodi ine
sindine Ambuye wanu?" Iwo adayankha: "Indedi! Ife tili
kuchitira umboni." Kuti mwina mungadzanene, pa tsiku
louka kwa akufa kuti: "Ndithudi ife sitimadziwa china
chilichonse cha izi." 173. Kapena mwina mungadzanene kuti,
"Ndi makolo athu akale amene amapembedza milungu
ina pambali pa Mulungu. Ife tidali m'badwo wapambuyo
pawo. Kodi inu mutiononga chifukwa cha zimene adachita
anthu oipa?" 174. Motero Ife tili kulongosola chivumbulutso
chathu kuti iwo abwerere.

175. Ndipo awerengere iwo za nkhani ya munthu amene
Ife tidamupatsa zizindikiro zathu koma iye adazikana,
ndipo Satana adamutsatira ndipo iye adali mmodzi wa
anthu osochera. 176. Ndipo tikadafuna Ife tikadamukweza
iye, koma iye adaumirira moyo wa pa dziko lino lapansi ndi
kutsatira zilakolako zake. Motero iye akhoza kufanizidwa
ndi galu, amene ngati umupilikitsa, amatulutsa lilime
lake, kaya umusiya yekha iye amalitulutsabe. Limenelo
ndi fanizo la anthu amene amakana zizindikiro zathu.
Motero auze nkhanizi kuti mwina iwo akhoza kuganiza

bwino. [177.] Choipa ndicho chifanizo cha anthu amene amakana chivumbulutso chathu, ndipo iwo amachimwira mizimu yawo yomwe. [178.] Aliyense amene Mulungu amamutsogolera, iye amatsogozedwa bwino ndipo aliyense amene Iye amusocheretsa, iye ndi olephera.

[179.] Ndithudi, Ife tanalenga majini ndi anthu ambiri kuti akalowe ku Gahena. Iwo ali ndi mitima imene sangathe kuzindikira, ali ndi maso amene sangathe kuona, ali ndi makutu amene sangathe kumva ayi. Iwo ali ngati ng'ombe. Iyai! Iwo ndi osochera kwambiri. Amenewa! Ndi nkhutukumve. [180.] Mulungu ali ndi mayina abwino kwambiri. Motero muitaneni pa mayina amenewo ndipo asiyeni iwo amene amaononga ulemerero wa mayina ake. Iwo adzalangidwa chifukwa cha zimene adali kuchita. [181.] Ndipo pakati pa iwo amene tidawalenga, alipo anthu amene amalangiza choonadi ndipo amachita chilungamo. [182.] Iwo amene amakana chivumbulutso chathu, Ife tidzawagwira pang'onopang'ono ndi chilango chathu popanda iwo kuzindikira. [183.] Ndimawapatsa nthawi, ndithudi, chikonzero changa ndi chokhwima.

[184.] Kodi iwo saganizira? Mulibe misala mwa m'bale wawo. Iye ndi mchenjezi basi. [185.] Kodi iwo sayang'ana mu Ufumu wa kumwamba ndi wa dziko lapansi ndi zonse zimene Mulungu adazilenga kuti aone ngati ndi mapeto a moyo wawo? Kodi ndi uthenga uti pambuyo pa uwu umene iwo adzakhulupirire? [186.] Aliyense amene Mulungu wamusocheza palibe wina amene angamutsogolere ndipo Iye amawasiya kuchita zinthu mwakhungu poswa malamulo. [187.] Iwo amakufunsa iwe za ola lomaliza kuti lidzadza liti? Nena, "Amene adziwa za tsikuli ndi Ambuye

wanga. Palibe amene adzaulule nthawi yake kupatula Iye
yekha.” Lidzalemetsa kumwamba ndi dziko lapansi. Ilo
silidzadza kwa inu kupatula mwadzidzidzi. Iwo alikufunsa
ngati iwe umadziwa zambiri za olali. Nena, “Kuzindikira
za tsikuli kuli kwa Mulungu yekha koma anthu ambiri
sadziwa.” 188. Nena, “Ine ndilibe mphamvu yopeza
zinthu, kapena kupewa mavuto kupatula ndi chifuniro
cha Mulungu. Ine ndikadakhala wodziwa chilichonse
chobisika ndikadadzichulukitsira chuma ndipo palibe
choipa chimene chikadandipeza. Ine sindine wina aliyense
ayi koma wopereka chenjezo ndi wobweretsa nkhani
yabwino kwa anthu okhulupirira.”
189. Iye ndiye amene adakulengani inu kuchokera
kwa munthu mmodzi ndipo kuchokera kwa munthu
ameneyu adamulengera mkazi wake, kuti akhoza kupeza
chisangalalo pokhala naye. Ndipo pamene iye amagona
naye, iye adatenga pakati pamene ananyamula mosavutika.
Koma pamene panakula, onse awiri amapempha Ambuye
wawo: “Ngati Inu mutatipatsa mwana wabwino ndithudi
ife tidzakhala othokoza.” 190. Koma pamene akawapatsa
mwana wabwino, iwo amakhazikitsa milungu ina pambali
pa Iye kuthokoza pa zimene wawapatsa. Alemekezeke
Mulungu kuposa zimene akumphatikiza nazo. 191. Kodi iwo
akukhazikitsa milungu ina pambali pa Mulungu weni weni
imene siingathe kulenga zina zilizonse koma kuti nayonso
ndi yolengedwa? 192. Palibe chimene ingawathandize ayi
ndiponso iyo siingathe kudzithandiza yokha. 193. Ndipo
ngati iwe uwaitana kunjira yoyenera iwo sadzakutsatira
ayi. Ndi chimodzimodzi kwa iwe kaya uwaitana kapena
ukhala chete. 194. Ndithudi iwo amene mumawapembedza

powonjezera pa Mulungu weniweni ndi akapolo ngati inu
nomwe. Motero aitaneni ndipo akuyankheni ngati zimene
munena ndi zoonadi.
195. Kodi iwo ali ndi miyendo yoti angayendere? Kodi ali
ndi manja oti angagwire china chilichonse? Kapena ali ndi
maso oti angaonere? Kapena ali ndi makutu oti angamvere?
Nena, "Itanani milungu yanu yabodza ndipo pangani
chiwembu chanu pa ine ndipo musandipatse mpumulo
ayi." 196. Ndithudi Mtetezi wanga ndi Mulungu amene
wavumbulutsa Buku ndipo Iye ndi Mtetezi wa anthu a
chilungamo. 197. Ndipo iwo amene mumawapembedza
powonjezera pa Iye sangathe kukuthandizani inu ndiponso
sangathe kudzithandiza iwo eni. 198. Ndipo ngati iwe
uwaitanira ku njira yoyenera, sakumva ayi ndipo udzawaona
ali kukuyang'ana iwe koma sakuona ai.
199. Onetsa kukhululukira, lamulira zabwino ndipo
uwapewe anthu osadziwa. 200. Ndipo ngati Satana akuyesa
iwe, thawira kwa Mulungu. Ndithudi Iye ndi wakumva ndi
wodziwa. 201. Ndithudi iwo amene amaopa Mulungu, ngati
maganizo oipa adza kwa iwo kuchokera kwa Satana, iwo
amakumbukira ndipo amaona kuunika. 202. Koma abale
awo, iwo amawalowetsa mu uchimo ndipo salekerera.
203. Ndipo ngati iwe siubweretsa chozizwitsa iwo amati,
"Kodi ndi chifukwa chiani siunabweretse?" Nena, "Ine
ndimatsatira chokhacho chimene chavumbulutsidwa kwa
ine kuchokera kwa Ambuye wanga." Uwu ndi umboni
wochokera kwa Ambuye wanu, malangizo ndi madalitso
kwa anthu okhulupirira. 204. Ndipo pamene Korani
ilakatulidwa, mverani ndipo khalani chete kuti mulandire
madalitso. 205. Ndipo kumbukira Ambuye wako ndi lilime

lako, mwa iwe wekha, modzichepetsa ndi mwamantha
ndiponso mosakweza mawu m'mawa ndi masana ndipo
usakhale ngati iwo a unyizi. 206. Ndithudi iwo amene ali
ndi Ambuye wako sanyada pogwira ntchito yopembedza
Mulungu koma amamulemekeza Iye ndipo amagunditsa
phumi zawo pamaso pake.

Sura 8 • Al-Anfâl

# Anfal

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Iwo akukufunsa iwe za katundu amene mumapeza
mukamenya nkhondo. Nena: "Mwini wake wa katundu
uyu ndi Mulungu ndi Mtumwi. Motero muopeni Mulungu
ndipo yanjanani pakati panu ndipo mverani Mulungu
ndi Mtumwi wake ngati inu ndinu okhulupirira."
2. Okhulupirira enieni ndi okhawo, amene ngati dzina
la Mulungu litchulidwa, amachita mantha m'mitima
mwawo ndipo pamene mavesi ake awerengedwa kwa iwo,
iwo amaonjezera chikhulupiriro chawo ndipo amaika
chikhulupiriro chawo mwa Ambuye wawo. 3. Amene
amapitiriza mapemphero ndipo amapereka mwaulere gawo
lina la zinthu zimene tawapatsa. 4. Iwo ndiwo amene ali
okhulupirira enieni. Kwa iwo kuli maudindo olemekezeka
amene ali ndi Ambuye wawo ndiponso chikhululukiro ndi
mphotho yolemekezeka.
5. Monga momwe Ambuye wako adakutulutsa m'nyumba

yako ndi choonadi ndipo, ndithudi, gulu lina la okhulupirira
sadakondwe ndi icho. 6. Kutsutsana ndi iwe pa choonadi
chimene chinadza ngati kuti iwo anali kuperekedwa ku
imfa pamene iwo anali kuona. 7. Ndi pamene Mulungu
adalonjeza gulu lina pakati pa magulu awiri, ilo ndi lanu
ndipo inu mudakonda kuti mukhale ndi gulu lija lopanda
zida koma Mulungu adafuna kukwaniritsa chilungamo
ndi mawu ake ndi kudula maziko ya anthu osakhulupirira.
8. Kuti choonadi chikhoza kupambana ndi kuthetsa bodza
ngakhale kuti anthu osakhulupirira anali kudana nazo.

9. Ndi pamene inu mudapempha thandizo la Ambuye
wanu ndipo Iye adakuyankhani: "Ine ndikuthandizani
ndi angelo chikwi chimodzi m'magulumagulu otsatana."
10. Mulungu anafuna kukusangalatsani chabe kuti mitima
yanu ikhazikike. Ndipo palibe kupambana kupatula
kochokera kwa Mulungu. Ndithudi Mulungu ndi
Wamphamvu ndi Wanzeru. 11. Pamene adakubweretsani
inu tulo ngati mtendere kuchokera kwa Iye ndipo
adakutumizirani mvula kuchokera kumwamba kuti
ikutsukeni ndi kukuyeretsani ku uve wa Satana ndi
kulimbikitsa mitima yanu ndi mapazi anu. 12. Pamene
Mulungu ananena ndi angelo kuti: Ndithudi Ine ndili
ndi inu ndipo limbikitsani anthu amene akhulupirira.
Ine ndidzakhazikitsa mantha m'mitima ya anthu
osakhulupirira, motero amenyeni m'makosi mwawo ndipo
konkhonthani zala zawo za kumanja ndi za kumapazi.
13. Ichi ndi chifukwa chakuti iwo sanamvere Mulungu ndi
Mtumwi wake. Ndipo aliyense amene samvera Mulungu ndi
Mtumwi wake, ndithudi, Mulungu ndi wolanga kwambiri.

14. Ichi ndi chilango motero chilaweni ndipo, ndithudi,
anthu osakhulupirira chawo ndi chilango chakumoto.
15. Oh inu anthu okhulupirira! Pamene mukumana ndi
magulu a nkhondo a anthu osakhulupirira musathawe.
16. Ndipo aliyense amene adzathawe patsiku limeneli
kupatula ngati kuli kukonzekera nkhondo kapena
kubwerera ku gulu lake, iye adzaputa mkwiyo wa Mulungu.
Ndipo Gahena idzakhala mudzi wake ndipo malowa ndi
oipa kukhalako.
17. Inu simunawaphe ai koma Mulungu ndiye amene
anawapha. Iwe siudaponye pamene udaponya koma
Mulungu ndi amene adaponya kuti akhoza kuyesa
okhulupirira ndi mayesero oyenera ochokera kwa Iye.
Ndithudi Mulungu ndi wakumva ndi wodziwa chili chonse.
18. Ichi, ndipo ndithudi, Mulungu amafoketsa ziwembu za
anthu osakhulupirira. 19. Ngati inu mufunsa chiweruzo,
tsopano chiweruzo chadza kwa inu ndipo ngati inu musiya
kuchita zoipa zidzakhala bwino kwa inu ndipo ngati inu
mubwerera, Ifenso tidzabwerera ndipo magulu anu a
nkhondo, ngakhale kuti ndi ochuluka, sadzakuthandizani
china chilichonse ndipo, ndithudi, Mulungu ali kumbali ya
anthu okhulupirira.
20. Oh inu anthu okhulupirira! Mverani Mulungu ndi
Mtumwi wake ndipo musamutaye ayi pamene inu muli
kumva. 21. Ndipo musakhale ngati iwo amene amati:
"Tamva"; pamene iwo sanamve. 22. Ndithudi! Zolengedwa
za moyo zimene zili zoipa kwambiri pamaso pa Mulungu
ndizo zimene zili zosamva, zosalankhula ndi izo zimene
sizizindikira. 23. Ngakhale Mulungu akadadziwa ubwino
umene uli mwa iwo, ndithudi, Iye akadawapanga kumva

koma ngakhale Iye akadawapanga kuti azimva, iwo
akadabwerera m'mbuyo ndi kukana choonadi.
24. Oh inu anthu okhulupirira! Yankhani Mulungu
ndi Mtumwi wake pamene akukuitananani ku chimene
chikupatsani inu moyo ndipo dziwani kuti Mulungu
amaima pakati pa munthu ndi mtima wake. Ndipo,
ndithudi, nonse mudzasonkhanitsidwa kudza kwa Iye.
25. Ndipo opani mayesero amene sabwera kwa anthu oipa
okha koma kwa inu nonse ndipo dziwani kuti Mulungu ndi
wokhwimitsa chilango chake.
26. Ndipo kumbukirani pamene inu mudali ochepa
ndipo mumaganizidwa kuti munali opanda mphamvu
m'dziko ndipo mudali kuopa kuti mwina anthu
akulandani. Koma Iye adakupatsani malo otetezedwa
okhala ndi kukulimbikitsani ndi chithandizo chake ndipo
adakupatsani zinthu zabwino kuti muzimuyamika. 27.
Oh inu anthu okhulupirira! Musamunyenge Mulungu
ndi Mtumwi ndipo musachite chinyengo pamene muli
nkudziwa pophwanya malonjezo anu. 28. Ndipo dziwani
kuti chuma chanu ndi ana anu ndi mayesero ndipo kuti,
ndithudi, kwa Mulungu kuli mphotho yaikulu.
29. Oh inu anthu okhulupirira! Ngati inu mumvera ndi
kuopa Mulungu, Iye adzakupatsani nzeru zodziwira
chabwino ndi choipa ndipo adzakukhululukirani machimo
anu ndipo Mulungu ndiye Mwini chuma chochuluka.
30. Ndi mmene anthu osakhulupirira adakupangira
chiwembu choti akugwire kuti ukhale mndende kapena
kukupha kapena kukuchotsa m'dziko lako. Iwo amachita
chiwembu koma Mulungu, nayenso amakonza chiwembu
chake, ndipo Mulungu ndi wopambana pokonza chiwembu.

31. Ndipo pamene chivumbulutso chathu chilakatulidwa
kwa iwo, iwo amati: “Ife tamva kale ndipo ngati ife
tikanafuna, tikhoza kunena cholingana nacho. Izi si
zina koma nkhani zopanda pake za anthu akale.” 32.
Ndi pamene iwo adanena kuti, “Oh Ambuye! Ngati
ichi ndi chivumbulutso choonadi chochokera kwa Inu,
gwetsani pamwamba pathu miyala kuchokera kumwamba
kapena tipatseni chilango chowawa.” 33. Ndipo Mulungu
sakadawalanga iwo pamene iwe unali pakati pawo ndipo
Iye sadzawalanga pamene iwo ali kupempha chikhululukiro
chake. 34. Kodi Mulungu asawalange iwo pamene iwo akhala
ali kuletsa ena kuti alowe mu Mzikiti Wolemekezeka
ngakhale kuti iwo alibe udindo woteteza Mzikitiwo? Palibe
outeteza kupatula okhawo amene amaopa Mulungu, koma
ambiri a iwo sadziwa. 35. Mapemphero awo mu Mzikiti
wolemekezeka sadali china chili chonse koma miluzu ndi
kuomba m’manja basi, motero lawani chilango chifukwa
inu simunali kukhulupirira.

36. Ndithudi iwo amene sakhulupirira, amaononga
chuma chawo ndi cholinga choletsa anthu kutsatira njira
ya Mulungu. Motero iwo adzapitirira kumwaza chuma
chawo; koma pomaliza iwo adzanong’oneza bombono.
Ndipo adzagonjetsedwa. Ndipo iwo amene sakhulupirira
adzasonkhanitsidwa ku Gahena. 37. Kuti Mulungu asiyanitse
pakati pa anthu oipa ndi abwino ndi kuwaika anthu oipa
wina pamwamba pa mnzake, ndipo adzawaunjika onse
pamodzi ndi kuwaponya ku Gahena. Awa! Ndiwo amene
ali olephera.

38. Nena kwa anthu osakhulupirira kuti ngati iwo
asintha njira yawo, zochimwa zawo zonse zakale

zidzakhululukidwa. Koma ngati iwo apitiririrabe kuchimwa,
zitsanzo za anthu akale, amene Mulungu adawaononga,
zikhale phunziro lawo. 39. Menyanani nawo mpaka pamene
kusakhulupirira ndi kupembedza mafano kutha ndipo
chipembedzo cha Mulungu chikhazikitsidwa ponseponse
koma ngati iwo asiya, ndithudi Mulungu akuona zochita
zawo zonse. 40. Koma ngati iwo sakumvera, dziwa kuti
Mulungu ndi Mtetezi wako. Iye ndi Mtetezi wabwino ndi
Mthandizi wabwino.

41. Ndipo dziwani kuti pa katundu yense amene mupeza
pa nkhondo, ndithudi gawo limodzi pa magawo asanu ndi
la Mulungu ndi Mtumwi ndi abale ake ndi ana a masiye,
anthu osauka ndi a paulendo, ngati inu mukhulupirira mwa
Mulungu ndi m'chivumbulutso chathu chimene tidatumiza
kwa kapolo wathu ndi tsiku lamayeso, tsiku limene magulu
awiri a nkhondo adakumana. Ndipo Mulungu ali ndi
mphamvu pa chilichonse.

42. Ndi pamene inu mudali tsidya lino la dambo ndi
pamene anthu osakhulupirira adali tsidya ilo ndi magareta
mmunsi mwanu. Ngakhale inu mukadagwirizana za malo
okumana, inu mukadalephera kukwaniritsa chipanganocho
koma Mulungu adafunitsitsa kuti akwaniritse zonse
zimene adalamulira kuti aliyense amene adalembedwa kuti
adzaonongeka, aonongeke pamene atalandira malangizo
ooneka ndipo kuti iwo amene adalembedwa kuti asafe
akhale ndi moyo atalandira malangizo ooneka. Ndithudi
Mulungu ndi wakumva ndi wodziwa. 43. Pamene Mulungu
adakuonetsa m'maloto ako ngati gulu laling'ono. Akadakhala
kuti adakuonetsa iwe kuti ndi gulu lalikulu, ndithudi
iwe ukadagwa mphwayi ndipo ukadavutika popereka

malamulo. Koma Mulungu adakupulumutsa. Ndithudi Iye
amadziwa zinthu zonse zimene zili m'maganizo mwanu.
44. Ndi pamene mudakumana nawo, Mulungu adakuonetsani
ngati ochepa m'maso mwanu ndipo anakuonetsani iwo inu
ngati ochepa m'maso mwawo kuti Mulungu akwaniritse
lamulo lake, limene anakhazikitsa kale, ndipo ndi kwa
Mulungu kumene zinthu zonse zimabwerera.
45. Oh inu anthu okhulupirira! Ngati mukumana ndi
gulu la nkhondo limbikani ndipo kumbukirani dzina la
Mulungu kwambiri kuti mupambane. 46. Ndipo mverani
Mulungu ndi Mtumwi wake ndipo musatsutsane wina
ndi mnzake chifukwa mudzakhumudwa ndi kuchita ulesi,
ndipo piririrani. Ndithudi Mulungu ali pamodzi ndi anthu
opirira. 47. Ndipo musakhale ngati iwo amene amachoka
m'nyumba mwawo modzitukumula ndi kudzionetsera kwa
anthu ndi kuwaletsa anthu kutsatira njira ya Mulungu,
ndipo Mulungu amadziwa zonse zimene iwo amachita.
48. Ndi pamene Satana adakometsa ntchito zawo
zopusa nati, "Palibe munthu wina aliyense amene
adzakugonjetsani inu lero, ndithudi ine ndidzakhala
pafupi kukuthandizani inu." Koma pamene magulu awiri a
nkhondo adakumana, iye adathawa ndipo anati: "Ndithudi
ine ndilibe nanu ntchito. Ndithudi ine ndaona zimene
inu simungathe kuziona. Ndithudi ine ndiopa Mulungu
chifukwa chilango chake ndi choopsya." 49. Pamene anthu
a chinyengo pamodzi ndi anthu amene m'mitima mwawo
mudali matenda adati: "Anthu awa ali kunyengedwa
ndi chipembedzo chawo." Koma aliyense amene aika
chikhulupiriro chake mwa Mulungu, ndithudi, Mulungu
ndi Wamphamvu ndi Wanzeru.

50. Iwe ukadawaona angelo pamene amachotsa mizimu
ya anthu osakhulupirira! Iwo amamenya pa nkhope ndi pa
misana yawo nati: “Lawani ululu wa moto wa ku Gahena.”
51. “Ichi ndi chifukwa cha zimene manja anu adatsogoza.
Ndipo ndithudi, Mulungu sapondereza akapolo ake.”
52. Monga anthu a Farao ndi iwo amene adalipo kale,
iwo adakana zizindikiro za Mulungu, ndipo Mulungu
adawalanga chifukwa cha kulakwa kwawo. Ndithudi
Mulungu ndi wamphamvu ndipo amakhwimitsa chilango.
53. Ichi ndi chifukwa chakuti Mulungu sasintha madalitso
amene amapereka kwa anthu mpaka pamene iwo asintha
makhalidwe awo, ndipo ndithudi, Mulungu ndi wakumva
ndi wodziwa. 54. Monga anthu a Farawo ndi iwo amene
adalipo kale, iwo sadakhulupirire uthenga wa Ambuye
wawo kotero Ife tidawaononga chifukwa cha zolakwa zawo
ndipo Ife tidamiza anthu a Farawo chifukwa onse adali
osalungama.
55. Ndithudi zolengedwa za moyo zimene ndi zoipitsitsa
pamaso pa Mulungu ndi anthu osakhulupirira ndipo iwo
sadzakhulupirira. 56. Iwo ndiwo amene iwe umapanga nawo
mapangano koma iwo amaphwanya mapangano awo nthawi
zonse ndipo iwo saopa Mulungu. 57. Ngati iwe uwapambana
pomenyana nawo nkhondo, alange kwambiri kuti ukhoza
kuthamangitsa iwo amene ali kumbuyo kwawo kuti akhoza
kuphunzira. 58. Ngati iwe uopa chinyengo chochokera
kwa anthu, nawenso abwezere mwawubwino machitidwe
omwewo. Ndithudi Mulungu sakonda anthu aupandu.
59. Ndipo anthu osakhulupirira asaganize kuti akhoza
kuthawa chilango. Ndithudi iwo sadzatha kudzipulumutsa.
60. Ndipo akonzekereni iwo mwamphamvu, mmene

mungathere, kuopseza adani a Mulungu ndi adani
anu ndiponso ena amene inu simuli kuwadziwa koma
Mulungu amawadziwa. Ndipo chili chonse chimene
mudzaononga mu njira ya Mulungu chidzabwezedwa
kwa inu ndipo inu simudzaponderezedwa. 61. Koma ngati
iwo afuna kukhazikitsa mtendere, nanunso khazikitsani
mtendere ndipo khulupirirani mwa Mulungu. Ndithudi
Iye ndi wakumva ndi wodziwa. 62. Ndipo ngati iwo afuna
kukunyenga ndithudi Mulungu ndi wokwanira kwa iwe.
Iye ndiye amene adakulimbikitsa pokupatsa chithandizo
chake ndi anthu okhulupirira. 63. Ndipo Iye wayanjanitsa
mitima yawo. Ngati iwe ukadawononga zinthu zonse
za padziko lapansi iwe siukadatha kuyanjanitsa mitima
yawo ayi koma Mulungu waiyanjanitsa. Ndithudi Iye ndi
Wamphamvu ndi Wanzeru.

64. Oh iwe Mtumwi! Mulungu ndi wokwanira kwa iwe
ndi kwa anthu okhulupirira amene amakutsatira iwe. 65. Oh
iwe Mtumwi! Alimbikitse anthu okhulupirira kuti amenye
nkhondo. Ngati pali anthu makumi awiri opilira pakati
panu, iwo adzagonjetsa anthu mazana awiri; ndipo ngati
pali anthu zana limodzi, iwo adzagonjetsa anthu chikwi
chimodzi cha anthu osakhulupirira chifukwa iwo ndi
anthu amene sazindikira. 66. Mulungu tsopano wachepetsa
vuto lanu chifukwa Iye adziwa kuti pakati panu pali anthu
ofoka. Motero ngati pali anthu zana limodzi opilira pakati
panu iwo adzagonjetsa anthu mazana awiri, ndipo ngati
pali anthu chikwi chimodzi, iwo adzagonjetsa anthu zikwi
ziwiri mwachifuniro cha Mulungu. Ndipo Mulungu ali
pamodzi ndi anthu opirira.

67. Sikoyenera kuti Mtumwi akhale ndi akapolo a

nkhondo mpaka iye atamenya nkhondo ndi kupambana
m'dziko. Inu mufuna kupeza zinthu zabwino za m'dziko
lino koma Mulungu akukufunirani za m'dziko limene
lili nkudza. Mulungu ndi wamphamvu ndi wanzeru.
68. Pakadakhala kuti padalibe lamulo lakale lochokera kwa
Mulungu, inu mukadalangidwa kwambiri chifukwa cha
zinthu zimene mwatenga. 69. Ndipo idyani zinthu zabwino
zololedwa zimene mwazipeza pa nkhondo ndipo opani
Mulungu. Ndithudi Mulungu amakhululukira ndipo ndi
wachisoni chosatha.
70. O Iwe Mtumwi! Nena kwa iwo amene mwawagwira
ukapolo, "Ngati Mulungu adziwa ubwino m'mitima
mwanu, Iye adzakupatsani zinthu zabwino kuposa zimene
mwalandidwa ndipo adzakukhululukirani machimo anu.
Mulungu amakhululukira ndipo ndi Wachisoni chosatha."
71. Koma ngati iwo afuna kukunyenga iwe, iwo adamunyenga
kale Mulungu. Motero wakupatsa iwe mphamvu kuti
uwapambane iwo. Ndipo Mulungu ndi wodziwa ndi
Waluntha.
72. Ndithudi iwo amene adakhulupirira ndi kusamuka
ndipo anapilira ndi kumenya nkhondo ndi chuma chawo ndi
iwo eni m'njira ya Mulungu ndipo ndi iwo amene adawasunga
ndi kuwathandiza, amenewa adzakhala a bwenzi a wina
ndi mnzake. Iwo amene akhulupirira koma sadasamuke
mwa njira iliyonse iwe ulibe udindo pa iwo pokhapokha
ngati iwo asamuka. Koma ngati iwo afuna chithandizo cha
chipembedzo ndi udindo wako kuwathandiza kupatula
anthu amene ali ndi pangano logwirizana pakati pa inu
ndi iwo ndipo Mulungu amaona ntchito zanu zonse.
73. Ndipo anthu osakhulupirira ndi abwenzi wina ndi

mnzake. Ndipo ngati inu simuchita chimodzimodzi
mudzakhala chisokonezo ndi kuponderezana m'dziko
ndiponso chionongeko chachikulu.
74. Ndipo iwo amene adakhulupirira ndipo adasamuka
ndipo adamenya nkhondo molimbika mu njira ya
Mulungu, ndi iwo amene adawasunga ndi kuwathandiza
amenewo ndiwo okhulupirira enieni ndipo iwo adzalandira
chikhululukiro ndi zabwino zambiri. 75. Ndipo iwo amene
adakhulupirira pambuyo pake kale ndipo adasamuka ndi
kumenya nkhondo pamodzi ndi iwe, iwo ndi abale ako.
Koma ubale wa magazi amodzi umakhala woganiziridwa
polandira katundu malinga ndi malamulo a Mulungu amene
adaperekedwa. Ndithudi Mulungu amadziwa zinthu zonse.

Sura 9 • At-Tawbah

## At-Tauba

1. Chidziwitso ichi chikhazikitsa malire oikidwa ndi
Mulungu ndi Mtumwi wake, kwa anthu opembedza
mafano amene mwapanga nawo lonjezo. 2. Kotero yendani
mwa ufulu miyezi inayi m'dziko lonse. Koma muyenera
kudziwa kuti inu simungathawe Mulungu ndipo Mulungu
adzachititsa manyazi anthu osakhulupirira. 3. Chidziwitso
chochokera kwa Mulungu ndi Mtumwi wake kunka kwa
anthu onse pa tsiku la likulu kuti Mulungu ndi Mtumwi
wake alibe udindo pa anthu opembedza mafano. Motero
ngati inu mulapa zidzakhala zabwino kwa inu, koma ngati
mukana, dziwani kuti inu simungamuthawe Mulungu
ndipo auze anthu osakhulupirira za chilango chowawa.

4. Kupatula opembedza mafano amene mwapangana nawo
chipangano, ndipo sadakukhumudwitseni pa chilichonse
ndipo sadamthandize aliyense kulimbana ndi inu. Kotero
kwaniritsani chipangano chawo kufikira kunthawi yawo.
Ndithudi Mulungu amakonda amene amaopa.
5. Ndipo pamene masiku a miyezi yolemekezeka atha,
iphani anthu opembedza mafano paliponse pamene
muwapeza ndipo agwireni, azungulireni ndipo abisalireni
m'njira iliyonse. Koma ngati iwo alapa ndipo achita
mapemphero ndi kupereka msonkho wothandizira anthu
osauka, muwasiye. Ndithudi Mulungu ndi Wokhululukira
ndipo ndi Wachisoni chosatha. 6. Ndipo ngati munthu
opembedza mafano afuna chitetezo chako, muteteze
kuti akhoza kumva Mau a Mulungu; ndipo mukatero
muperekezeni kumalo a mtendere chifukwa iwo ndi anthu
osadziwa chilichonse.
7. Kodi pangakhale bwanji mgwirizano pakati pa Mulungu
ndi Mtumwi wake ndi anthu opembedza mafano kupatula
okhawo amene mudachita nawo lonjezo pafupi ndi Mzikiti
Wolemekezeka? Ngati iwo asunga malonjezo awo kwa
inu nanunso musunge malonjezo anu kwa iwo. Ndithudi
Mulungu amakonda amene amaopa. 8. Kodi pangakhale
bwanji mgwirizano pamene iwo akapambana, salemekeza
ubale kapena mgwirizano umene uli pakati panu? Ndi
pakamwa pawo amakukondweretsani inu koma mitima
yawo imakana ndipo ambiri a iwo ndi ochita zoipa. 9. Iwo
agula ndi chivumbulutso cha Mulungu zinthu za mtengo
wochepa ndipo amaletsa anthu kunjira yake. Zoipa ndizo
zimene iwo amachita. 10. Akakhala okhulupilira, iwo
salemekeza mgwirizano wa ubale kapena wa chipangano!

Iwo ndiwo amene amaphwanya malamulo. 11. Koma ngati
iwo alapa, apitiliza mapemphero ndipo apereka msonkho
wothandizira anthu osauka, iwo ndiye kuti ndi abale
anu m'chipembedzo. Ife timalongosola chivumbulutso
mwatsatane tsatane kwa anthu ozindikira.
12. Koma ngati iwo aphwanya kulumbira kwawo pambuyo
pa pangano lawo ndipo atukwana chipembedzo chanu,
menyani atsogoleri osakhulupirira chifukwa, ndithudi,
zolumbira zawo zilibe tanthauzo, kuti mwina asiye
kuchita zoipa. 13. Kodi inu simudzamenyana nawo anthu
amene adaphwanya malonjezano awo ndi kutsimikiza
zomuthamangitsa Mtumwi pamene iwo ndiwo amene
adakuyambani? Kodi mukuwaopa iwo? Ndithudi Mulungu
ndiye amene muyenera kumuopa ngati inu ndinu anthu
okhulupirira. 14. Amenyeni kuti Mulungu awalange iwo
ndi manja anu ndi kuwachititsa manyazi, ndi kukupatsani
inu kupambana ndi kuchiza mitima ya anthu okhulupirira.
15. Ndi kuchotsa mkwiyo m'mitima mwawo. Mulungu
amakhululukira aliyense amene Iye wamufuna. Mulungu
ndi wodziwa ndipo ndi wanzeru.
16. Kodi inu mukuganiza kuti mudzasiyidwa nokhanokha
pamene Mulungu sadawayese iwo amene ali pakati panu,
amene adamenya nawo nkhondo mwachamuna ndipo
sadachite ubwenzi ndi wina kupatula Mulungu ndi Mtumwi
wake ndi anthu okhulupirira? Mulungu amadziwa zimene
mumachita.
17. Sikoyenera kuti anthu opembedza mafano azisamala
Mizikiti ya Mulungu pamene iwo avomereza okha kuti
ndi anthu osakhulupirira. Ntchito zawo zidzakhala
zopanda pake ndipo ku moto wa ku Gahena ndiko kumene

iwo adzakhale. 18. Mizikiti ya Mulungu idzasamalidwa ndi okhawo amene akhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza ndipo amapitiriza mapemphero ndipo amapereka msonkho wothandizira anthu osauka ndipo saopa wina aliyense koma Mulungu yekha. Ndi amenewa amene amaganiziridwa kuti amatsata njira yoyenera.
19. Kodi mumaganiza kuti kupereka madzi kwa anthu a Hajji ndi kuyang'anira Mzikiti Wolemekezeka kukhala chimodzimodzi ndi iwo amene akhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza ndipo amalimbikira m'njira ya Mulungu? Iwo si ofanana pamaso pa Mulungu. Ndipo Mulungu satsogolera anthu ochita zoipa. 20. Iwo amene adakhulupirira, nasamuka, ndipo analimbikira m'njira ya Mulungu ndi chuma chawo pamodzi ndi iwo eni, iwo ali ndi udindo waukulu pamaso pa Mulungu. Iwo ndiwo opambana. 21. Ambuye wawo ali kuwauza nkhani yabwino ya chisomo kuchokera kwa Iye ndipo kuti Iye ndi wokondwa ndi ya minda imene ili ndi chisangalalo chosatha. 22. Iwo adzakhala mmenemo mpaka kalekale. Ndithudi kwa Mulungu kuli mphotho yaikulu.

23. Oh inu anthu okhulupirira! Musasandutse atate ndi abale anu kukhala atetezi anu ngati iwo akonda kusakhulupirira kuposa chikhulupiriro. Ndipo aliyense wa inu amene achita ubwenzi ndi anthu otere ndi olakwa.
24. Nena, "Ngati atate anu, ana anu, abale anu, akazi anu, a pabanja lanu, chuma chimene mwapeza, katundu wa malonda amene muopa kuonongeka, ndi nyumba zimene mukonda ndi zopambana kwambiri kwa inu kuposa Mulungu ndi Mtumwi wake ndi kulimbikira mu njira

yake, ndiye dikirani mpaka pamene Mulungu abweretsa
chilamulo chake. Mulungu satsogolera anthu ochita zoipa.”
25. Ndithudi Mulungu wakhala ali kukupambanitsani
m’malo ankhondo osiyanasiyana ndi nkhondo ya tsiku
la Hunain, pamene inu mudasangalala ndi kuchuluka
kwanu koma sikudakuthandizeni chilichonse ndipo dziko
linakupanikizani, ngakhale kuti lidali lalikulu, linaoneka
laling’ono kwa inu ndipo munatembenuka kuthawa.
26. Ndipo Mulungu adatsitsa chisomo chake pa Mtumwi
wake ndi kwa okhulupirira ndipo adatumiza Asirikali amene
inu simudawaone ndipo analanga anthu osakhulupirira.
Amenewa ndiwo malipiro a anthu osakhulupirira. 27. Ndipo
pambuyo pake Mulungu adzavomera kulapa kwa aliyense
amene Iye wamufuna. Ndipo Mulungu ndi wokhululukira
ndi wachisoni chosatha. 28. Oh inu anthu okhulupirira!
Ndithudi anthu opembedza mafano ndi uve. Motero
asayandikire pafupi ndi Mzikiti Wolemekezeka chikatha
chaka chino ndipo ngati inu muopa umphawi, Mulungu,
ngati afuna, adzakulemeretsani inu kuchokera ku chuma
chake. Ndithudi Mulungu amadziwa chilichonse ndipo ndi
Wanzeru.

29. Menyananinawo anthu amene sakhulupirira mwa
Mulungu ndi tsiku lomaliza kapena iwo amene saletsa
zimene Mulungu ndi Mtumwi wake adaletsa kapena
savomeleza chipembedzo choonadi amene ali pakati pa
anthu amene adapatsidwa Buku, mpaka pamene iwo alipira
msonkho umene amapereka anthu amene sali Asilamu
ndipo adzichepetsa. 30. Ndipo Ayuda amati: “Ezra ndiye
mwana wa Mulungu” pamene Akhirisitu amati “Mesiya
ndiye mwana wa Mulungu.” Izi ndi nkhambakamwa. Iwo

amangotsatira zimene anthu opembedza mafano akale amanena. Matemberero a Mulungu akhale pa iwo. Kodi iwo akusocheretsedwa bwanji kunjira yoyenera?
31. Iwo anasandutsa Abusa ndi atsogoleri awo a mpingo kukhala Ambuye mowonjezera pa Mulungu ndi Messiya, mwana wa Maria, ngati Mulungu pamene iwo adalamulidwa kuti asapembedze wina aliyense koma Mulungu mmodzi yekha basi. Kulibe mulungu wina koma Iye yekha. Kuyamikidwa ndi kulemekezedwa kukhale kwa Iye kuposa zonse zimene adazikhazikitsa mowonjezera pa Iye.
32. Iwo amafuna kuzimitsa Muuni wa Mulungu ndi pakamwa pawo koma Mulungu sadzalora kupatula kuti Muuni wake ukhazikike ngakhale kuti anthu osakhulupirira
amadana nawo. 33. Iye ndiye amene adatumiza Mtumwi
wake ndi chilangizo ndi chipembedzo choonadi kuti chipambane zipembedzo zina zonse ngakhale kuti anthu opembedza mafano amadana nazo.
34. Oh inu anthu okhulupirira! Ndithudi ambiri a Atsogoleri a Chiyuda ndi Abusa a Chikhristu amadya chuma cha anthu mu njira yosalungama ndipo amatsekereza kunjira ya Mulungu. Ndi iwo amene amasonkhanitsa golide ndi siliva ndipo sapereka chumacho mu njira ya Mulungu,
auzeni za chilango chowawa. 35. Pa tsiku limene chuma
chawo chidzasungunulidwa ndi moto wa ku Gahena, ndipo ndi icho mphumi zawo, nthiti zawo, ndi misana yawo idzalembedwa ,“Izi ndi zomwe munali kuzisonkhanitsa nokha. Tsopano lawani zomwe mudali kusonkhanitsa.”
36. Ndithudi chiwerengero cha miyezi kwa Mulungu ndi khumi ndi iwiri ndipo inakhazikitsidwa ndi Mulungu, pa tsiku limene Iye adalenga kumwamba ndi dziko lapansi.

Pa iyi, miyezi inayi ndi yopatulika. Ichi ndi chipembedzo
choonadi, motero musadzipondereze nokha m'miyezi
imeneyi, ndipo menyanani nawo anthu osakhulupirira
monga momwe amenyana nanu. Koma dziwani kuti
Mulungu ali pamodzi ndi anthu olungama. 37. Kusintha,
ndithudi, ndi kuonjezera kusakhulupirira, motero anthu
osakhulupirira amasokera chifukwa iwo amaikhazikitsa
chaka chino ndi kusintha m'chaka china kuti akonze miyezi
imene Mulungu waletsa ndi kusandutsa imene inaletsedwa
kukhala yololedwa. Ntchito zawo zoipa zimawasangalatsa.
Ndipo Mulungu satsogolera anthu osakhulupirira.
38. Oh inu anthu okhulupirira! Kodi mwatani? Kodi ndi
chifukwa chiani zimati zikanenedwa kwa inu kuti muyende
m'njira ya Mulungu, inu mumakondweretsedwa ndi
zadziko? Kodi inu mukonda moyo wa dziko lapansi kuposa
moyo umene uli nkudza? Chisangalalo chadziko lapansi ndi
chochepa kufanizira ndi moyo umene uli nkudza. 39. Ngati
inu simupita nawo ku nkhondo, Iye adzakulangani ndi
chilango chowawa ndipo adzaika m'malo mwanu anthu ena
ndipo inu simungathe kumupweteka Iye chifukwa Mulungu
ali ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse. 40. Ngati
inu simudzathandiza Mtumwi, Mulungu adamuthandiza
iye pamene anthu osakhulupirira adamupilikitsa, mmodzi
mwa awiri, pamene iwo adali kuphanga ndipo iye ananena
kwa mnzake kuti: Usade nkhawa, ndithudi Mulungu ali
nafe. Ndipo Mulungu adatsitsa chisomo chake pa iye ndipo
adamulimbikitsa ndi Asirikali omwe sadawaone ndipo Iye
adapanga mawu a anthu osakhulupirira kukhala a pansi,
ndi a Mulungu kukhala a pamwamba. Ndithudi Mulungu
ndi Wamphamvu ndi Wanzeru.

41. Pitani kunkhondo kaya muli opepukidwa kapena
olemedwa. Limbikirani kwambiri ndi chuma chanu
pamodzi ndi inu nomwe m'njira ya Mulungu. Ichi
ndi chinthu chabwino kwa inu ngati mukadadziwa.
42. Kukadakhala kuti zinali zinthu zopezako mosavuta
kapena ulendo waufupi, iwo akadakutsatira iwe koma
ulendo unali wautali kwa iwo ndiponso wovuta ndipo iwo
akanalumbira m'dzina la Mulungu kuti: "Ife tikadatha,
ndithudi, tikadapita nanu. Iwo akudziononga okha ndipo
Mulungu amadziwa kuti iwo ndi abodza."
43. Mulungu akukhululukire iwe: Kodi ndi chifukwa
chiyani unawapatsa chilolezo mpaka pamene iwo onena
zoona anaoneka kwa iwe poyera ndi kuwadziwa onama?
44. Iwo amene amakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku la
chimaliziro sadzapempha kuti asamenyane nawo nkhondo
ndi chuma chawo ndiponso iwo eni. Ndipo Mulungu
amadziwa anthu olungama. 45. Ndi okhawo amene
sakhulupilira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza, iwo amene
m'mitima mwawo muli chikaiko, amene amapempha
chilolezo. Motero chifukwa cha chikaiko, iwo ndi
wosakhazikika. 46. Iwo akadafuna kuti apite kunkhondo,
ndithudi, akadaikonzekera koma Mulungu sadafune kuti
apite nawo ndipo adawakhalitsa, ndipo zidanenedwa kwa
iwo, "Khalani pamodzi ndi anthu otsalira."
47. Ngati iwo akadapita nawe kunkhondo, iwo
sakadaonjezera china chilichonse koma chisokonezo,
ndipo iwo akadayenda uku ndi uku pakati panu kufalitsa
zoipa ndipo ena mwa inu akanawamvera. Ndipo Mulungu
amawadziwa anthu ochita zoipa. 48. Ndithudi iwo adakonza
chiwembu chokuukira ndipo anasokoneza chili chonse

mpaka pamene chilungamo chinadza ndipo ulamuliro wa
Mulungu unakhazikika angakhale iwo anali kudana nawo.
49. Ndipo pakati pawo pali iye amene amati: "Ndipatseni
chilolezo ndipo musandiike m'mayesero." Ndithudi iwo
adagwa kale m'mayesero. Ndipo ndithudi, moto wa ku
Gahena uli kukuta anthu osakhulupirira. 50. Ngati upeza
chabwino, iwo chimawanyansa koma ngati mavuto adza
pa iwe, iwo amati: "Ife tidadziteteza kale." Ndipo iwo
amabwerera m'mbuyo mosangalala. 51. Nena, "Palibe
chimene chingationekere ife kupatula chokhacho chimene
Mulungu analamula kuti chidze pa ife. Iye ndiye Ambuye
wathu." Ndipo mwa Mulungu, anthu onse okhulupirira
ayike chikhulupiliro chawo. 52. Nena, "Kodi muli kudikira
kuti chimodzi mu zinthu ziwiri zabwino kwambiri kuti
chitionekere? Pamene ife tiri kuyembekezera kuti Mulungu
adzakubweretserani chilango chochokera kwa Iye kapena
kuchokera ku manja athu. Motero dikirani nafenso tiri
kudikira pamodzi ndi inu."
53. Nena, "Perekani mwachifuniro chanu kapena
mokakamizidwa, koma palibe chimene chidzalandiridwa
kuchokera kwa inu. Ndithudi inu ndinu anthu ochita
zoipa." 54. Palibe chimene chaletsa kuti zopereka zawo
zilandiridwe kupatula kuti iwo sanakhulupilire mwa
Mulungu ndi Mtumwi wake ndipo iwo samabwera ku
mapemphero kupatula mwaulesi ndipo samapereka
zopereka zawo kupatula modandaula. 55. Motero usalole
kuti chuma chawo kapena ana awo kuti akudabwitse.
Cholinga cha Mulungu ndikufuna kuwalanga ndi izi
m'moyo uno ndipo kuti mizimu yawo idzachoke pamene
iwo ali osakhulupirira. 56. Iwo amalumbira M'dzina la

Mulungu kuti iwo ali pamodzi ndi inu pamene iwo sali
ndi inu ayi, koma iwo ndi anthu a mantha. 57. Ngati iwo
akadapeza pothawira kapena phanga kapena pobisala, iwo
akadathamangira kumeneko mosacheuka.
58. Ndipo pakati pawo alipo ena amene amanena zoipa
za iwe pa kagawidwe ka katundu. Ngati iwo atapatsidwa
gawo la katunduyo, iwo amasangalala, koma ngati
sapatsidwa china chilichonse, amakwiya kwambiri..
59. Iwo akadangokhutitsidwa ndi zinthu zimene Mulungu
ndi Mtumwi wake adawapatsa, ndi kunena kuti: "Mulungu
ndi okwanira kwa ife. Mulungu adzatipatsa zabwino
zake ndiponso Mtumwi wake. Ife timpempha Mulungu."
60. Ndithudi chopereka chaulele chiperekedwe kwa
anthu osauka, osowa ndi iwo amene amagwira ntchito
yosonkhanitsa zoperekazo, ndi iwo amene angolowa
chipembedzo cha Chisilamu, kuombola akapolo, anthu
amene apanikizidwa ndi ngongole, amene agwira ntchito ya
Mulungu ndi munthu wa paulendo; limeneli ndi lamulo la
Mulungu. Mulungu ndi wodziwa chilichonse ndi Wanzeru.
61. Ndipo pakati pawo alipo ena amene amanyoza
Mtumwi ponena kuti: "Iye amangomvera chili chonse."
Nena: "Iye amamvetsera zinthu zimene zili zabwino
kwa inu. Iye amakhulupirira mwa Mulungu ndipo Iye
amakhulupilira anthu okhulupirira, ndipo iye ndi madalitso
kwa ena a inu amene amakhulupilira." Koma iwo amene
amanyoza Mtumwi wa Mulungu adzakhala ndi chilango
chowawa. 62. Iwo amalumbira M'dzina la Mulungu kwa inu
kuti akukondweretseni chabe, koma ndi kwabwino kuti
iwo akondweretse Mulungu ndi Mtumwi wake ngati iwo
ndi okhulupilira. 63. Kodi iwo sadziwa kuti aliyense amene

apikisana ndi Mulungu ndi Mtumwi wake, ndithudi, iye adzakhala ku moto wa ku Gahena nthawi zonse? Kumeneko ndiko kunyozedwa kwakukulu.

64. Anthu a chinyengo aopa kuti mwina mutu ungavumbulutsidwe wonena za iwo. Nena, "Nyozani! Koma, ndithudi, Mulungu adzaonetsa poyera zonse zimene muli kuopa." 65. Ngati uwafunsa, iwo amati: "Ife timangocheza ndi kusewera basi." Nena: "Kodi ndi Mulungu, chivumbulutso chake ndi Mtumwi wake amene munali kunyoza?" 66. Musawilingule ai. Inu mudakana pambuyo pokhulupirira. Ngati Ife tikhululukira gulu lina mwa inu, Ife tidzalanga gulu lina pakati panu chifukwa iwo anali anthu ochita zoipa.

67. Anthu achinyengo, amuna ndi akazi, onse ndi chimodzimodzi. Iwo amalamulira zinthu zoipa ndi kuletsa zimene zili zabwino ndiponso iwo amaumila. Iwo amuiwala Mulungu, motero nayenso wawaiwala. Ndithudi anthu a chinyengo ndi anthu wochita zoipa. 68. Mulungu walonjeza anthu a chinyengo, amuna ndi akazi ndiponso anthu osakhulupirira moto wa ku Gahena ndipo iwo adzakhala kumeneko mpaka kalekale. Chimenechi ndi chilango chowayeneradi. Mulungu wawatemberera ndipo chawo chidzakhala chilango chosatha. 69. Monga iwo amene adalipo inu musanadze, iwo adali ndi mphamvu zambiri zoposa inu ndipo adali ndi chuma chambiri ndi ana ochuluka. Iwo adasangalala ndi zawo pa kanthawi motero nanunso munasangalala ndi zanu pa kanthawi monga momwe iwo anasangalalira. Ndipo inu mwalowa m'masewera ndi kutaya nthawi monga momwe iwo amachita masewera ndi kutaya nthawi. Awa ndiwo amene

ntchito zawo zaonongeka m'moyo uno ndi m'moyo umene
uli nkudza. Amenewa ndiwo amene ali olephera. 70. Kodi
iwo sanamve mbiri ya anthu akale? Za anthu a Nowa, a
Thamoud, a Abrahamu ndi anthu a ku Midiyani ndi a
mizinda yoonongeka? Kwa iwo kunadza Atumwi awo ndi
zizindikiro zooneka. Motero Mulungu sadawalakwire ayi
koma iwo adadzilakwira okha.

71. Anthu okhulupirira, amuna ndi akazi ndi othandizana
wina ndi mnzake. Iwo amalamulira zabwino ndi kuletsa
zoipa, amapitiriza mapemphero ndipo amapereka
msonkho wothandiza anthu osauka ndipo amamvera
Mulungu ndi Mtumwi wake. Mulungu adzaonetsa chisoni
chake pa iwo. Ndithudi Iye ndi Wamphamvu ndi Wanzeru.
72. Mulungu wawalonjeza okhulupirira amuna ndi akazi,
minda imene pansipake pamayenda mitsinje yamadzi,
kuti adzakhalamo mpaka kalekale ndi Nyumba zokongola
za m'munda wa Edeni. Koma chisomo chachikulu ndi
chisangalalo cha Mulungu. Kumeneko ndiko kupambana
kweni kweni.

73. Oh Iwe Mtumwi! Limbana kwambiri ndi anthu
osakhulupirira ndiponso ndi anthu a chinyengo ndipo
uwaonetsere nkhanza. Gahena ndiyo idzakhala mudzi
wawo. Ndipo malo oipa kwambiri ndi amenewo. 74. Iwo
amalumbira pali Mulungu kuti sanena china chilichonse.
Koma iwo adalankhula mawu oonetsa kusakhulupirira
ndipo iwo sanakhulupirire atalowa Chisilamu. Ndipo iwo
anatsimikiza kuchita zimene sadathe kuzichita. Ndipo iwo
sanathe kupeza chifukwa choyenera kuti atero kupatula
kuti Mulungu ndi Mtumwi wake adawalemeretsa ndi
katundu wake. Ngati iwo alapa, zikhala zabwino kwa iwo,

koma ngati atembenuka, ndithudi, Mulungu adzawalanga
ndi chilango chowawa pa dziko lino ndi mdziko limene
lili nkudza. Iwo alibe wina aliyense Wowateteza padziko
lapansi.
75. Ndipo pakati pawo pali ena amene anachita lonjezo
ndi Mulungu ponena kuti: “Ngati Iye atipatsa ife chuma,
ndithudi, tidzapereka zopereka ndipo tidzakhala m’gulu
la anthu abwino.” 76. Koma pamene Mulungu adawapatsa
kuchokera ku chuma chake, iwo anayamba umbombo
ndipo adatembenuka mophwanya lonjezo lawo. 77. Motero
Iye adawalanga pokhazikitsa chinyengo m’mitima mwawo
mpaka pa tsiku limene iwo adzakumana Naye, chifukwa
chakuphwanya kwawo zimene analonjeza kwa Iye ndi
chifukwa chakulankhula kwawo kwabodza. 78. Kodi iwo
sadziwa kuti Mulungu amadziwa zinsinsi zawo ndi maupo
awo a m’nseri ndi kuti Mulungu amadziwa zobisika?
79. Iwo amene amaononga mbiri ya anthu okhulupirira
amene amapereka mosaumilizidwa ndi iwo amene
sanapeza chopereka kupatula chimene ali nacho, motero
iwo amanyoza. Mulungu adzawabwezera mtozo wawo.
Motero chawo chidzakhala chilango chowawa. 80. Kaya
iwe uwapemphera chikhululukiro kapena usawapemphere,
ngakhale iwe utawapemphera chikhululukiro kokwana
makumi asanu ndi awiri, Mulungu sadzawakhululukira
chifukwa iwo sanakhulupilire mwa Mulungu ndi Mtumwi
wake. Ndipo Mulungu satsogolera anthu ochita zoipa.
81. Iwo amene adasiyidwa m’mbuyo adasangalala chifukwa
cha kukhala kwawo pambuyo pa Mtumwi wa Mulungu,
iwo amadana ndi kukamenya nkhondo ndi chuma chawo
ndiponso iwo eni yokhazikitsa ulamuliro wa Mulungu ndipo

iwo adati, “Musapite ku nkhondo chifukwa kuli kutentha kwambiri.” Nena, “Moto wa ku Gahena ndi wotentha kwambiri,” iwo akadangozindikira. 82. Motero iwo aseke pang’ono ndi kudzalira kwambiri ngati malipiro a ntchito zimene adachita. 83. Ngati Mulungu akubweretserani gulu lina la iwo ndipo akapempha chilolezo kuti atuluke; nena, “Inu simudzatuluka ndi ine kapena kukamenya nkhondo ndi adani pamodzi ndi ine. Inu munasangalatsidwa kukhala ku nyumba kwanu pa nthawi yoyamba ndipo khalani pamodzi ndi anthu otsalira m’mbuyo.” 84. Iwe usampempherere aliyense wa iwo amene afa, ndipo usadzaime pa manda ake. Ndithudi iwo sanakhulupirire mwa Mulungu ndi Mtumwi wake ndipo adafa ali ochita zoipa.

85. Ndipo usalole kuti chuma ndi ana awo kuti zikudabwitse iwe. Cholinga cha Mulungu ndi kuwalanga iwo ndi izi m’moyo uno ndikuti mizimu yawo idzachoke ali anthu osakhulupirira. 86. Ndipo pamene Mutu uvumbulutsidwa kuwauza kuti akhulupirire mwa Mulungu ndi kuti amenye nkhondo limodzi ndi Mtumwi, anthu olemera pakati pawo amakupempha kuti, asakamenye nawo ndipo amati: “Tisiye ife tikhale pamodzi ndi anthu okhala m’mbuyo.” 87. Iwo amasangalala kuti akhale limodzi ndi iwo amene adakhalira m’mbuyo! Mitima yawo ndi yomatidwa, motero iwo sazindikira. 88. Koma Mtumwi ndi amene adakhulupirira pamodzi ndi iye, analimbikira ndipo adamenya nkhondo pogwiritsa ntchito chuma chawo pamodzi ndi iwo eni. Awa ndiwo amene wawasungira zinthu zabwino ndipo ndiwo amene adzakhale opambana. 89. Awa ndiwo amene Mulungu wawakonzera minda yothiriridwa ndi mitsinje

yoyenda pansi, mmene adzakhalemo mpaka kalekale. Kumeneku ndiko kupambana kwakukulu.

90. Ndipo iwo amene adali ndi zifukwa kuchokera ku gulu
la anthu a mchipululu adabwera, kuti apatsidwe chilolezo
choti asakamenye nkhondo ndipo iwo amene adanama
kwa Mulungu ndi kwa Mtumwi wake adakhala kumudzi.
Chilango chowawa chidzadza pa iwo amene sakhulupirira.
91. Palibe mlandu kwa anthu ofoka, odwala ndi iwo amene
alibe chopereka, ngati ali ndi cholinga chabwino kwa
Mulungu ndi Mtumwi wake. Anthu angwiro sadzaimbidwa
mlandu ayi! Ndipo Mulungu amakhululukira ndipo ndi
Wachisoni chosatha. 92. Ndipo palibe cholakwa kwa iwo
amene adadza kwa iwe kuti uwapezere choti akwere ndipo
iwe udati: "Sindingapeze choti ndikutengerenimo" ndipo
iwo amabwerera kwawo m'maso mwawo muli misozi
yodandaula kuti sadapeze zoti apereke. 93. Mlandu uli ndi
anthu olemera, omwe amapempha kuti asakamenye nawo
nkhondo. Iwo amasangalala kukhalira limodzi ndi iwo
amene atsalire m'mbuyo ndipo Mulungu waphimba mitima
yawo kotero iwo sadziwa.

94. Iwo adzapereka zodandaula zawo pamene mudza kwa
iwo. Nena: "Inu musanene china chili chonse chifukwa
ife sitidzakukhulupirirani. Mulungu watiuza kale nkhani
zanu. Mulungu ndi Mtumwi wake adzayang'ana ntchito
zanu zonse. Ndipo pomaliza inu mudzabwerera kwa
Iye amene amadziwa zinthu zobisika ndi zooneka,
ndipo Iye adzakuuzani zonse zimene munkachita."
95. Iwo adzalumbira kwa inu M'dzina la Mulungu pamene
mubwerera kwa iwo kuti muwasiye okha. Motero asiyeni
okha chifukwa iwo ndi uve chifukwa cha ntchito zawo.

Ndipo yawo ndi Gahena, omwe ndi malipiro antchito
zimene ankachita. 96. Iwo adzalumbira kwa inu pofuna
kuti musangalale nawo. Koma ngati inu musangalala nawo
ndithudi Mulungu sasangalalira anthu ochita zoipa.
97. Maarabu amene amakhala m'chipululu ndiwo oipa
kwambiri posakhulupirira ndi m'chinyengo, ndipo ndi
oyenera kusadziwa malire amene Mulungu wavumbulutsa
kwa Mtumwi wake. Ndipo Mulungu amadziwa zinthu zonse
ndipo ndi Wanzeru. 98. Pakati pa Maarabu amene amakhala
m'chipululu, alipo ena amene amaganiza kuti zonse zimene
amapereka kuti ndi dipo lolipira mlandu ndipo amadikira
kuti mupeze tsoka. Kwa iwo kukhale tsoka loipa! Ndipo
Mulungu amamva zonse ndipo amadziwa chilichonse.
99. Pakati pa Maarabu ena a m'chipululu pali amene
amakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza, ndipo
amaona zopereka zawo m'njira ya Mulungu ngati zinthu
zowabweretsa kufupi ndi Mulungu ndi mapemphero a
Mtumwi. Ndithudi zimenezo zidzawabweretsa kufupi.
Ndipo Mulungu adzawalowetsa iwo ku chisomo chake.
Ndithudi Mulungu ndi wokhululukira ndi wachisoni
chosatha.
100. Ndipo iwo amene adalowa Chisilamu poyamba,
kuchokera ku gulu limene lidachoka ku Makka ndi
ku Medina, ndi ena amene anawatsatira. Mulungu ndi
wosangalala kwambiri ndi iwo monga momwe iwo ali
osangalala ndi Iye. Iye wawakonzera minda yothiriridwa ndi
madzi a mitsinje yoyenda pansi pake kumene adzakhalako
mpaka kalekale. Kumeneku ndiko kupambana kwakukulu.
101. Ndipo pakati pa Maarabu amene amakhala m'chipululu
amene akuzungulira iwe, ena ndi anthu a chinyengo,

chimodzi modzi anthu ena a ku Medina. Iwo amanena zabodza ndipo ndi a chinyengo. Iwe siuwadziwa koma Ife timawadziwa. Ife tidzawalanga kawiri ndipo pambuyo pake adzabwezedwa ku chilango chachikulu.

102. Ena alipo amene avomera zoipa zawo, iwo asakaniza ntchito zawo zabwino ndi ntchito zawo zoipa. Mwina Mulungu adzawalandira kulapa kwawo. Ndithudi Mulungu ndi wokhululukira ndi Mwini chisoni chosatha.
103. Landira chopereka chaulele kuchokera ku chuma chawo kuti uwayeretse nacho ndipo uwapempherere, ndithudi mapemphero ako adzawapatsa mpumulo ndipo Mulungu amamva zonse ndipo amadziwa zinthu zonse. 104. Kodi iwo sadziwa kuti Mulungu amalandira kulapa kwa akapolo ake ndipo amavomera zopereka zawo ndipo kuti ndi Mulungu yekha amene amakhululukira ndi kuvomera kulapa, ndi Mwini chisoni chosatha? 105. Nena, "Chitani monga momwe mufunira! Mulungu adzaona ntchito zanu ndi Mtumwi wake ndi anthu okhulupirira. Ndipo inu mudzabwezedwa kwa Iye amene amadziwa zobisika ndi zoonekera. Ndipo Iye adzakuuzani zonse zimene mumachita." 106. Ndipo ena akudikira chilamulo cha Mulungu, kaya Iye adzawalanga kapena adzawakhululukira. Mulungu ndi wodziwa chili chonse ndi wanzeru zonse.

107. Ndipo iwo amene anamanga Mzikiti ndi cholinga choyambitsa chisokonezo ndi kulimbikitsa kusakhulupirira ndi kugawanitsa anthu okhulupirira, poyembekezera kwa amene adachita nkhondo ndi Mulungu ndi Mtumwi wake pambuyo pake, iwo adzalumbira kuti cholinga chawo chidali chabwino. Mulungu achitira umboni kuti iwo ndi onama. 108. Usapemphere m'menemu. Ndithudi Mzikiti

umene udamangidwa ndi cholinga chomuopa Mulungu
kuchokera tsiku loyamba ndi woyenera kuti iwe upemphere
mmenemo. Mmenemo muli anthu okonda kudziyeretsa.
Ndipo Mulungu amakonda iwo amene amadziyeretsa.
109. Kodi amene waika maziko a nyumba yake ndi cholinga
choopa Mulungu ndikufuna chisangalalo chake ndi
wabwino kapena iye amene waika maziko a nyumba yake
m'mphepete mwadzenje limene likugumukira dothi lake
kugwera pamodzi ndi nyumbayo kumoto wa ku Gahena?
Mulungu satsogolera anthu ochita zoipa. 110. Nyumba
imene amanga siidzasiya kukhala yachinyengo ndi
yokaikitsa m'mitima mpaka pamene mitima yawo idulidwa
m'timagawomagawo. Ndipo Mulungu ndi wodziwa ndi
wanzeru.

111. Ndithudi Mulungu wagula miyoyo ya anthu
okhulupilira ndi chuma cha pa mtengo wakuti chawo
chidzakhale Paradiso. Iwo amamenya nkhondo munjira
ya Mulungu kotero amapha ndi kuphedwa. Ili ndi lonjezo
loonadi kwa Iye limene lidzakwaniritsidwa ndipo liri
m'Buku la Chipangano chakale, Chipangano chatsopano
ndi Korani. Kodi ndani amene amakwaniritsa lonjezo
lake kuposa Mulungu? Iwo ali kusangalala ndi mgwirizano
omwe mwachita. Kumeneko ndiko kupambana kwakukulu.
112. Iwo amene amalapa zoipa zawo kwa Mulungu, iwo
amene amapembedza, amayamika, amasala zilakolako
zawo, amawerama, amagwada, amagwetsa mphumi zawo
pansi, amalamulira zabwino, amaletsa zoipa ndi amene
amasunga malire a Mulungu. Motero lalikira nkhani
yabwino kwa anthu okhulupirira.

113. Sizili zoyenera kwa Mtumwi ndi anthu okhulupirira

kuwapemphera chikhululukiro anthu opembedza mafano
ngakhale kuti iwo ndi a chibale awo pambuyo podziwika
kwa iwo kuti iwo ndi anthu a kumoto. 114. Sichinali cholinga
cha Abrahamu kuwapempherera abambo wake koma
chifukwa cha lonjezo limene iye adachita nawo. Koma
pamene iye adazindikira kuti abambo wake adali mdani
wa Mulungu, iye adawakana iwo. Ndithudi Abrahamu
adali wodzichepetsa ndi munthu woleza mtima. 115. Ndipo
Mulungu sadzasocheretsa anthu amene wawatsogolera
pokhapokha Iye wawafotokozera zonse zimene ayenera
kuzipewa, Ndithudi Mulungu amadziwa chinthu china
chilichonse. 116. Ndithudi Mulungu! Ndiye Mwini Ufumu wa
Kumwamba ndi dziko lapansi, Iye ndiye amene amapereka
moyo ndi imfa. Ndipo kupatula Mulungu, inu mulibe wina
amene angakutetezeni kapena kukuthandizani.

117. Mulungu adakhululukira Mtumwi, anthu osamuka
ndi anthu a ku Medina, amene adamtsatira iye pa nthawi
ya mavuto, pamene ena adali pafupifupi kutaya mitima.
Koma Iye adavomera kulapa kwawo. Ndithudi Iye, kwa
iwo, ndi Wachifundo ndi Wachisoni chosatha. 118. Iye
adakhululukira anthu atatu amene adasiyidwa m'mbuyo,
mpaka pamene kwa iwo dziko, ngakhale ndi lalikulu, linali
lochepa ndipo mizimu yawo idapanikizika ndipo iwo
adakhulupirira kuti kudalibe komuthawira Mulungu koma
kupita kwa Iye. Motero Iye adavomera kulapa kwawo.
Ndithudi Mulungu ndiye amene amavomera kulapa ndipo
ndi wachisoni chosatha.

119. Oh inu anthu okhulupirira! Muopeni Mulungu
ndipo khalani pamodzi ndi iwo amene amanena zoona.
120. Sikunali koyenera kwa anthu a ku Medina ndi Maarabu

a mchipululu a m'mbali mwawo kutsalira m'mbuyo mwa Mtumwi wa Mulungu kapena kukonda miyoyo yawo kuposa moyo wake. Icho ndi chifukwa chakuti iwo savutika ndi ludzu kapena kutopa kapena njala mu njira ya Mulungu kapena sachita chinthu chowanyasa anthu osakhulupirira kapena kubweretsa mavuto pa adani koma kudalembedwa kwa iwo kuti ndi ntchito yabwino. Ndithudi Mulungu saononga mphotho ya a anthu ochita zabwino. 121. Ndipo iwo sapereka chopereka chochepa kapena chochuluka kapena kudutsa dambo lililonse koma kuti zidalembedwa ngati mphotho zabwino kwa iwo ndi kuti Mulungu adzawalipire zabwino zimene ankachita.

122. Si chinthu chabwino kuti anthu onse okhulupirira apite ku nkhondo nthawi imodzi. Pa gulu lili lonse, kagulu kochepa kokha kayenera kupita kuti kakhoza kuphunzira ndipo kuti iwo amene atsalira akhoza kudzachenjeza anthu awo pamene adza kwa iwo kuti achenjere.

123. Oh inu anthu okhulupirira! Menyanani nawo anthu onse osakhulupilira amene ali pafupi ndi inu ndipo iwo apeze nkhanza kwa inu ndipo dziwani kuti Mulungu ali pamodzi ndi anthu olungama. 124. Ndipo nthawi zonse pamene mutu uli kuvumbulutsidwa, ena a iwo amanena kuti: "Kodi ndani wa inu amene chikhulupiriro chake chaonjezeka chifukwa cha mutu uwu?" Akakhala iwo okhulupirira, uwaonjezere chikhulupiriro chawo ndipo amasangalala. 125. Koma iwo amene m'mitima mwawo muli matenda, udzangoonjezela chikaiko pamwamba pa chikaiko chawo, ndipo iwo adzafa ali osakhulupirira. 126. Kodi iwo saona kuti amayesedwa kamodzi kapena kawiri chaka chili chonse? Komabe iwo safuna kulapa kapena

kuphunzira kuchokera kwa iwo. 127. Nthawi zonse pamene
mutu uvumbulutsidwa, iwo amayang'anitsitsana ndi
kufunsa kuti: "Kodi akukuonani wina aliyense?" Akatero
iwo amabwerera m'mbuyo. Mulungu watembenuza mitima
yawo, chifukwa iwo ndi anthu osazindikira.
128. Ndithudi kwadza kwa inu Mtumwi wochokera
pakati panu. Zimamudandaulitsa kuti mupeze mavuto.
Iye amafunitsitsa kuti inu mukhulupilire ndipo kwa anthu
okhulupirira iye ndi wachifundo ndi wachisoni chosatha.
129. Koma ngati iwo akana Nena, "Mulungu ndi wokwana
kwa ine. Kulibe Mulungu wina koma Iye yekha. Mwa Iye
ine ndaika chikhulupiliro changa ndipo Iye ndiye Ambuye
wa Mpando wa Chifumu."

Sura 10 • Yûnus

# Yunus

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Alif Lam Ra. Awa ndi mavesi a Buku la zinthu zanzeru
zenizeni. 2. Kodi n'chodabwitsa kwa anthu kuti Ife
tidavumbulutsa chivumbulutso kwa mmodzi wa iwo
ponena, "Pereka chenjezo kwa anthu ndipo uwauze nkhani
zabwino anthu okhulupirira kuti adzakhala ndi mpando
wapamwamba kwa Ambuye wawo?" Anthu osakhulupirira
adati: "Ndithudi uyu ndi wamatsenga enieni."
3. Ndithudi Ambuye wanu ndi Mulungu, amene m'masiku
asanu ndi limodzi adalenga kumwamba ndi dziko lapansi

ndipo anabuka pamwamba pa Mpando wachifumu,
nalamula zinthu zonse. Palibe wina amene adzalandira
ulamuliro wopepesa kwa Mulungu pokhapokha atalandira
chilolezo cha Mulungu. Ameneyo ndiye Mulungu Ambuye
wanu, mpembedzeni Iye. Kodi simudzakumbukira?
4. Kwa Iye nonse mudzabwerera. Lonjezo la Mulungu ndi
loona. Iye ndiye adayamba kulenga zolengedwa zonse
ndipo pomaliza adzazipatsanso moyo kuti adzawalipire
mwa chilungamo onse amene adakhulupirira mwa Iye
ndipo ankachita ntchito zabwino. Anthu osakhulupirira
adzamwa zakumwa zamadzi ogaduka ndi kulandira
chilango chowawa chifukwa chosakhulupirira.
5. Iye ndiye amene adalipanga dzuwa kukhala muuni ndi
mwezi kukhala wowala ndipo adazikonzera modutsa kuti
inu muzidziwa kuchuluka kwa zaka ndi chiwerengero. Iye
sadazilenge chabe izo koma mu choonadi. Iye amafotokoza
mawu ake momveka kwa anthu ake ozindikira. 6. Ndithudi
mukasinthidwe ka usiku ndi usana ndi zimene Mulungu
walenga kumwamba ndi dziko lapansi, muli zizindikiro
kwa anthu okana uchimo. 7. Ndithudi iwo ndi anthu amene
sayembekeza kuti adzakumana nafe ndipo amasangalala
ndi moyo wa m'dziko lapansi ndi kukhutitsidwa nawo
ndiponso amene salabadira mawu. 8. Iwo malo awo okhala
ndi kumoto chifukwa cha zoipa zimene anali kuchita.
9. Ndithudi iwo amene akhulupirira ndipo amachita ntchito
zabwino, Ambuye wawo adzawatsogolera m'chikhulupiriro
chawo. Mitsinje idzakhala ili kuyenda pansi pawo m'minda
ya mtendere. 10. Pemphero lawo mmenemo lidzakhala
loti; "Ndinu Woyera Ambuye!" Ndipo kulonjerana
kwawo kudzakhala koti: "Mtendere" ndipo kumapeto

kwa pempho lawo adzati: "Kuyamikidwa kukhale kwa
Mulungu, Ambuye wa chilengedwe."
11. Akadakhala kuti Mulungu amabweretsa msanga
chilango kwa anthu monga momwe iwo amafunira
zabwino kuti zidze mwansanga, nthawi yawo yofera
ikadakwaniritsidwa. Kwa iwo amene saopa kukumana ndi
Ife tidzawasiya mukusochera kwawo, akusowa chochita.
12. Pamene mavuto amadza pa munthu, iye amapemphera
kwa Ife mogona chanthiti, mokhala pansi kapena moimirira.
Koma tikangomuchotsera mavuto ake, iye amatsatila
njira zake kukhala ngati sadatipemphe kuti timuchotsere
mavuto omwe adamupeza. Kotero zidakongoletsedwa kwa
anthu oononga zimene anali kuchita.
13. Zoonadi Ife tidaononga mibadwo imene idalipo inu
musanadze, pamene iwo adachita zoipa, anawafikira
Atumwi awo ndi umboni weniweni koma iwo
sadakhulupilire, motero tidzawalipira anthu ochita
zoipa. 14. Ndipo Ife tidakupangani kukhala alowa mmalo
awo m'dziko lawo pambuyo pawo, kuti tione mmene inu
mungachitire.
15. Ndi pamene Mau athu awerengedwa kwa iwo
momveka, anthu amene salabadira zakukumana nafe
amanena kuti, "Bweretsa Buku la Korani losiyana ndi ili
kapena ulisinthe." Nena, "Siudindo wanga kusintha Buku
ili mwa chifuniro changa. Ndithudi ine ndimangotsatira
zokhazo zimene zavumbulutsidwa kwa ine. Ndithudi ine
ndimaopa chilango cha tsiku lalikulu ngati nditanyoza
Ambuye wanga." 16. Nena, "Mulungu akadafuna, ine
sindikadawerenga ilo kwa inu ndiponso Iye sakadakupatsani
inu nzeru zoti mulidziwe. Ndithu moyo wanga wonse

ndakhala ndili pakati panu, Bukuli lisadavumbulutsidwe.
Kodi simungathe kuzindikira?” 17. Kodi wolakwa kwambiri
ndani kuposa munthu amene amapeka bodza lokhudza
Mulungu kapena amene amakana Mau ake? Ndithudi
anthu ochita zoipa sadzapambana ayi.
18. Iwo amapembedza zinthu zina, osati Mulungu, zimene
sizingathe kuwapweteka kapena kuwathandiza ndipo
amati, “Izi zidzatilankhulira ife kwa Mulungu.” Nena, “Kodi
inu mukumuuza Mulungu za zinthu zimene Iye sazidziwa
zomwe zili kumwamba kapena pa dziko lapansi? Iye ndi
Woyera ndipo akhale wa pamwamba kuposa mafano awo.”
19. Mtundu wa anthu unali umodzi koma anasemphana
pambuyo pake. Ndipo kukanapanda kuti Mau a Ambuye
wako ananenedwa kale, mkangano wawo ukanathetsedwa.
20. Anthu osakhulupirira amanena kuti: “Kodi chifukwa
ninji chizindikiro sichinaperekedwe kwa iye kuchokera
kwa Ambuye wake?” Nena, “Mulungu yekha ndiye amene
amadziwa chilichonse chobisika. Dikirani, nanenso ndili
mmodzi mwa odikira.” 21. Ndipo tikawalawitsa anthu
mtendere pambuyo pa mavuto amene anawapeza, iwo
amayamba kukonza chiwembu chotsutsa chivumbulutso
chathu. Nena: “Mulungu ndi wa changu pokonza
chiwembu. Ndithudi Angelo athu ali kulemba zonse
zimene mumapanga za chiwembu.”
22. Iye ndiye amene amakuyendetsani pa mtunda ndiponso
pa nyanja mpaka pamene inu muli m’ngalawa ndipo
izo zimayendetsedwa ndi mphepo yabwino imene iwo
amasangalala nayo. Koma mphepo ya mkuntho imawafikira
ndipo mafunde amadza kwa iwo kuchokera ku mbali zonse
ndipo iwo amaganiza kuti yawapeza ndipo amapemphera

kwa Mulungu momuyeretsera chipembedzo chake. “Ngati
mutipulumutse ku mavuto awa, ife tidzakhala othokoza.”
23. Ndipo pamene Mulungu adawapulumutsa, iwo
adayamba kuchita zoipa pa dziko mopanda chilungamo.
Oh inu anthu! Zoipa zanu simuchitira wina aliyense koma
inu nokha. Chimenecho ndicho chisangalalo cha moyo wa
pa dziko lapansi ndipo pambuyo pake inu mudzabwerera
kwa Ife ndipo tidzakuuzani zonse zomwe mumachita.
24. Ndithudi chitsanzo cha moyo wadziko lapansi chili
ngati mvula imene timatsitsa kuchokera kumwamba ndipo
imameretsa zomera za pa dziko zimene amadya anthu
ndi nyama mpaka pamene dziko likongola ndi zomerazo.
Ndipo anthu ake amakhulupirira kuti amalipambana
ndipo lamulo lathu limadza pa izo nthawi ya usiku
kapena ya masana ndipo timaichita kukhala ngati mbewu
yokololedwa imene kunalibe dzulo. Mmenemo ndi mmene
timaululira chivumbulutso chathu kwa anthu oganiza.
25. Mulungu ali kuitanira ku Nyumba ya mtendere, ndi
kumutsogolera yemwe wamufuna kunjira yoyenera. 26. Kwa
iwo onse amene amachita zabwino adzapeza zabwino ndi
zoonjezerapo. Ndipo nkhope zawo sizidzakutidwa ndi
fumbi kapena kunyozedwa. Iwo ndi anthu a ku Paradiso,
komwe adzakhala mpaka kalekale. 27. Ndipo iwo amene
amachita zoipa, malipiro awo ndi oipa mofanana ndi zimene
adachita. Mnyozo udzawakuta ndipo iwo sadzakhala ndi
wina aliyense wowateteza ku chilango chochokera kwa
Mulungu. Ndipo nkhope zawo zidzaoneka ngati kuti
zidakutidwa ndi mbali ya mdima wa usiku. Iwo adzakhala
anthu a kumoto ndipo adzakhala kumeneko nthawi zonse.
28. Tsiku limene tidzawasonkhanitsa onse, Ife tidzati kwa

anthu opembedza mafano: “Khalani m’malo mwanu, inu
pamodzi ndi mafano anu.” Ife tidzawasiyanitsa wina ndi
mnzake ndipo mafano awo adzati kwa iwo: “Sindife amene
inu munali kupembedza ayi.” 29. “Akukwanira Mulungu
kukhala mboni pakati pa ife ndi inu. Ife sitidziwa kuti
munali kutipembedza!” 30. Kumeneko mzimu uliwonse
udzadziwa chimene unatsogoza. Iwo adzabwezedwa kwa
Mulungu, Ambuye wawo woona ndipo zidzawasokonekera
iwo zimene anali kupeka.

31. Nena, “Kodi ndani amakupatsani zinthu kuchokera
kumwamba ndi padziko lapansi? Kodi ndani amene
amapereka mphamvu yakumva ndi kuona? Kodi
ndani amatulutsa cha moyo kuchokera ku chakufa ndi
kutulutsa chakufa kuchokera mu chamoyo? Ndani amene
amalamulira zinthu zonse?” Onse adzanena kuti, “Ndi
Mulungu.” Nena, “Kodi inu simungaope Mulungu?”
32. Ameneyo ndiye Mulungu, Ambuye wanu woona. Kupatula
choonadi, kodi ndi chiyani chimene chingakhalepo osati
chisokonekero? Nanga ndi chifukwa chiyani inu muli
kusocheretsedwa? 33. Kotero ndi mmene liwu la Ambuye
wako latsimikizidwira kwa anthu ochita zoipa ndipo iwo
sadzakhulupirira.

34. Nena, “Kodi ena a mafano anu angalenge china chake
ndi kuchibwezeranso?” Nena, “Mulungu anayambitsa
chilengedwe ndipo adzachibwezeranso. Nanga ndi chifukwa
chiyani mukusocheretsedwa?” 35. Nena, “Kodi mafano anu
angakulondolereni ku choonadi?” Nena, “Mulungu yekha
ndiye amene angakulondolereni ku choonadi. Kodi ndani
amene ayenera kutsatidwa? Iye amene amakulondolerani
ku choonadi kapena iye amene sangathe chifukwa chakuti

nayenso afuna kuti atsogozedwe? Kodi mukusiyanitsa
bwanji?" 36. Ambiri a iwo satsatira china chilichonse koma
zongoganiza. Komatu nkhani zongoganiza sizithandiza mu
choonadi chilichonse. Ndithu Mulungu amadziwa zonse
zimene iwo amachita.
37. Sizingatheke kuti Korani iyi ikhale yopeka ndiponso
kuti siinachokere kwa Mulungu. Koma iyo imatsimikiza
zinthu zonse zimene zidavumbulutsidwa kale ndi
kufotokoza Mau a m'buku la Mulungu. Ilo ndi losakaikitsa
ndipo ndi lochokera kwa Ambuye wa zolengedwa zonse.
38. Kapena iwo amati "Iye walipeka!" Nena: "Nanunso
pekani mutu umodzi wolingana nalo ndipo itanani amene
mungathe kuwaitana osakhala Mulungu ngati muli
angwiro!" 39. Iyayi. Iwo ali kutsutsa zinthu zimene sadziwa
chilichonse cha izo pamene choona chake chisanafike kwa
iwo. Mmenemonso ndi mmene anthu akale adakanira.
Taonani zidali bwanji zotsatira za anthu ochita zoipa.
40. Ena a iwo amakhulupirira mu ilo pamene ena
sakhulupirira ayi. Ndipo Ambuye wako amawadziwa
kwambiri anthu owononga. 41. Ngati iwo akukana iwe,
nena: "Ine ndili ndi ntchito zanga ndipo nanunso muli
ndi ntchito zanu. Inu muli kutali ndi zimene ndikuchita
ndipo nanenso ndili kutali ndi zimene mukuchita."
42. Ena a iwo amakumvera iwe. Kodi iwe ungawapangitse
agonthi kuti amve ngakhale kuti safuna kuzindikira?
43. Ena a iwo amakuyang'ana iwe. Kodi iwe ungalangize
njira kwa anthu a khungu pamene saona china chilichonse?
44. Ndithudi Mulungu salakwira anthu koma kuti anthu eni
ake amadzipondereza okha.
45. Akumbutseni zatsiku limene adzawasonkhanitsa onse.

Tsiku limeneli adzaona ngati kuti adangokhala ora limodzi
lamasana. Iwo adzazindikirana wina ndi mnzake. Ndithudi
olephera adzakhala iwo amene adakana za kukumana ndi
Mulungu ndipo sanali otsogozedwa. 46. Kaya tikuonetsa
zina za zimene tawalonjeza kapena kukuchititsa kuti ufe,
ndi kwa Ife kumene onse adzabwerera ndipo Mulungu ndi
mboni pa zimene akuchita.
47. Ndithudi m'mbadwo uliwonse uli ndi Mtumwi
wake ndipo pamene Mtumwi wawo adza, nkhani yawo
idzaweruzidwa mwa chilungamo pakati pawo ndipo
sadzaponderezedwa.
48. Iwo amanena: "Kodi lonjezo limeneli
lidzakwaniritsidwa liti ngati ukunena zoona?" 49. Nena,
"Ine ndilibe mphamvu yopeza zabwino kapena kupewa
choipa chimene chingadze pa ine kupatula ndi chifuniro
cha Mulungu. M'badwo uliwonse uli ndi nthawi imene
idakhazikitsidwa kale. Ndipo pamene nthawi yawo idza,
iwo sadzatha kuichedwetsa kapena kuifulumizitsa."
50. Nena "Ndiuzeni! Ngati chilango chake chitadza pa
inu nthawi ya usiku kapena masana kodi ndi gawo liti
limene anthu ochita zoipa angalifulumize?" 51. Kodi inu
mudzakhulupirira pamene chidza pa inu? Nanga! Tsopano
siuja munali kuchifulumizitsa? 52. Ndipo kudzanenedwa
kwa anthu ochita zoipa! "Lawani chilango chosatha! Inu
simudzalipidwa china chilichonse kupatula zimene munali
kuchita."
53. Ndipo amakufunsa kuti uwauze: "Kodi ndizoona?"
Nena, "Indedi, pali Ambuye. Zimenezo ndi zoonadi ndipo
inu simungazithawe ayi." 54. Kukadakhala kuti munthu
aliyense wochita zoipa anali ndi zinthu zonse zimene zili

padziko lapansi ndipo amafuna kuzipereka ngati dipo loti
adziombolere, ndipo iwo akanamva chisoni m'mitima
yawo pamene akadaona chilango ndipo iwo adzaweruzidwa
mwachilungamo ndiponso sadzaponderezedwa ai.
55. Ndithudi mosakaika Mulungu ndiye Mwini wa
chilichonse chimene chili mlengalenga ndi padziko lapansi.
Ndithudi mosakaika lonjezo la Mulungu ndi loona. Koma
ambiri a iwo sadziwa. 56. Iye ndiye amene amapereka moyo
ndipo amaperekanso imfa, ndipo ndi kwa Iye kumene inu
nonse mudzabwerera.
57. Oh inu anthu! Chilangizo chabwino chadza kwa inu
kuchokera kwa Ambuye wanu, chochiritsa zimene zili
m'mitima mwanu, utsogoleri ndi madalitso kwa anthu
okhulupirira m'choonadi. 58. Nena, "M'chisomo ndi
M'chisoni cha Mulungu asiyeni asangalale. Chifukwa izi ndi
zabwino kuposa zimene akusonkhanitsa." 59. Ndiuzeni kodi
Mulungu wakufulumizirani chiani? Ndipo mwazisandutsa
zina kukhala zololedwa ndi zina zoletsedwa. Nena, Kodi
Mulungu wakulolani kapena mukumpekera zabodza?.
60. Kodi anthu amene amapeka mabodza okhudza Mulungu
amaganiza chiyani za tsiku la kuuka kwa akufa? Ndithudi
Mulungu ndi wabwino kwa anthu koma ambiri a iwo
sathokoza ayi.
61. Chilichonse chimene uzichita ndiponso gawo lililonse
limene uzilakatula la Korani ndipo chilichonse chimene
muzichita, Ife ndife mboni pa icho pamene muli kuchichita.
Palibe chobisika kwa Ambuye wanu, ngakhale chochepa
ngati nyerere padziko lapansi kapena kumwamba. Palibe
chaching'ono choposa ichi kapena chachikulu choposa ichi
chimene sichilembedwa mu Buku. 62. Mosakaika! Ndithudi

abwenzi a Mulungu ndipo amamukonda Iye kwambiri,
sadzakhala ndi mantha ndiponso sadzadandaula. 63. Iwo
amene adakhulupirira ndipo anali kuopa Mulungu. 64. Kwa
iwo ndi chisangalalo m'dziko lino ndiponso m'dziko limene
lili n'kudza. Palibe kusintha kulikonse m'Mau a Mulungu.
Kumeneko ndiko kupambana kwakukulu. 65. Ndipo mawu
awo asakukhumudwitse iwe. Ndithudi mphamvu zonse
Mwini wake ndi Mulungu. Iye ndi wakumva ndi wodziwa.
66. Mosakaika! Ndithudi Mulungu ndiye mwini wa zimene
zili kumwamba ndi dziko lapansi. Ndipo onse amene
amapembedza milungu yabodza satsatira china chilichonse
koma zinthu zopanda pake ndipo iwo amangopeka
mabodza. 67. Iye ndiye amene adakupangirani usiku kuti
muzipumula ndi usana kuti muziona. Ndithudi mu izi muli
zizindikiro kwa anthu amene amamva.

68. Iwo amanena kuti: "Mulungu wabereka mwana
wamwamuna." Mulungu ayeretsedwe ndi zimenezo. "Iye
ndi Wolemera. Zake ndi zonse zimene zili m'lengalenga ndi
pa dziko lapansi. Pa ichi inu mulibe umboni. Kodi mukunena
zinthu zokhudza Mulungu zimene simuzidziwa?" 69. Nena,
"Ndithudi iwo amene amapeka bodza lokhudza Mulungu
sadzapambana ayi." 70. Chisangalalo cha kanthawi kochepa
ka m'dziko lapansi ndipo ndi kwa Ife kumene adzabwerera
ndipo Ife tidzawalawitsa chilango chowawa chifukwa cha
kukana kwawo.

71. Ndipo awerengere iwo za nkhani ya Nowa pamene
iye adanena kwa anthu ake kuti: "Oh! Inu anthu anga!
Ngati muli kuipidwa ndi kukhala kwanga pakati panu
ndi kukukumbutsani mawu a Mulungu, dziwani kuti ine
ndaika chikhulupiliro changa mwa Mulungu motero inu

musonkhanitse zopanga zanu ndi mafano anu ndipo inu
musapange chiwembu mseri ayi. Gamulani chiweruzo
chanu pa ine ndipo musandipatse nthawi ayi.” 72. “Ndipo
ngati muyamba kusakhulupirira ine sindidakupempheni
mphotho. Mphotho yanga ili ndi Mulungu ndiponso
ndalamulidwa kuti ndikhale mmodzi mwa ogonjera
malamulo a Mulungu.” 73. Koma iwo adamukana. Ife
tidamupulumutsa Nowa pamodzi ndi iwo amene adali naye
m’chombo ndipo tinawapanga iwo kukhala olowa m’malo
padziko ndipo tidamiza onse amene adakana zonena zathu.
Ona, adali bwanji mapeto a anthu ochenjezedwa.
74. Zitatha izi, tidatumiza Atumwi ena kwa anthu awo.
Iwo adadza kwa iwo ndi zizindikiro zooneka koma iwo
sanali okhulupirira mzimene adazikana kale. Mmenemo
ndi mmene timadindira zidindo mitima ya anthu ochita
zinthu mopyora muyeso.
75. Pambuyo pake tinatumiza Mose ndi Aroni ndi
zizindikiro zathu kwa Farawo ndi nduna zake. Koma iwo
adadzikweza ndipo anali anthu oipa. 76. Pamene chidadza
choonadi kwa iwo kuchokera kwa Ife, iwo adati: “Ndithudi
awa ndi matsenga woonekereratu.” 77. Mose adati: “Kodi
inu mukunena choona pamene chakufikani kuti ndi
matsenga? Wamatsenga sapambana ai.” 78. Iwo adati:
“Kodi iwe wadza kuti utitembenuze m’zimene tidapeza
makolo athu akuchita ndi cholinga chakuti inu anthu awiri,
mukhale akuluakulu m’dziko? Ife sitikukhulupirirani anthu
awirinu.”
79. Ndipo Farawo adati: “Bweretsani wa amatsenga
aliyense wodziwa kwa ine.” 80. Pamene amatsenga adadza,
Mose adati kwa izo: “Ponyani zonse zimene mufuna

kuponya.” 81. Ndipo pamene adaponya pansi ndodo zawo
Mose adati: “Amenewa ndi matsenga ndipo Mulungu,
ndithudi, adzagonjetsa matsenga anu. Ndithudi Mulungu
savomera ntchito za anthu ochita zoipa kuti zipambane.”
82. Mulungu, ndi Mau ake, amakhazikitsa choonadi
ngakhale kuti anthu oipa sakondwera.
83. Palibe amene adamukhulupirira Mose kupatula ana
a anthu ake chifukwa chomuopa Farawo ndi nduna zake
kuti angawavutitse. Ndithudi Farawo adali wokakala moyo
m’dzikomo ndiponso adali m’modzi wa anthu oononga.
84. Mose adati: “Oh inu anthu anga! Ngati inu
mwakhulupirira mwa Mulungu, mudalire mwa Iye yekha,
ngati inu muli anthu okhulupirira.” 85. Iwo adati: “Timadalira
mwa Mulungu. Oh Ambuye wathu! Musalole kuti ife
tizunzike m’manja mwa anthu oipa.” 86. “Tipulumutseni
mwa chisomo chanu kwa anthu osakhulupirira.”
87. Tidavumbulutsa Mau athu kwa Mose ndi m’bale wake
ponena kuti: “Amangireni nyumba anthu anu m’dziko la
Aiguputo ndipo mupange nyumba zanu kukhala malo
opemphereramo. Pitirizani mapemphero ndipo muwauze
nkhani yabwino anthu okhulupirira.”
88. Ndipo Mose adati: “Ambuye wathu! Inu mwamupatsa
Farao ndi anthu ake zinthu zabwino ndi chuma m’moyo
uno, Ambuye wathu, kuti asocheretse anthu ku njira yanu.
Ambuye wathu! Onongani chuma chawo ndipo limbitsani
mitima yawo, kuti iwo asadzakhulupirire mpaka pamene
aona chilango chowawa.”
89. Mulungu adati: “Pempho lanu layankhidwa. Kotero
pitirizani kuyenda m’njira yoyenera nonse awiri ndipo
musatsatire njira ya anthu osadziwa.”

90. Ife tidatsogolera ana a Israyeli kuoloka nyanja. Farawo,
pamodzi ndi magulu ake a nkhondo, adawatsatira ndi
chiwembu ndiponso udani. Kufikira pamene anali kumira,
Farawo adati: "Ndikhulupirira kuti kulibe mulungu koma
Iye amene ana a Israyeli amamukhulupirira. Ndipo ine
ndili m'modzi wa odzipereka pogonjera." 91. "Chiyani?
Tsopano ndiye ukukhulupirira pamene iwe udanyoza kale
ndipo udali mmodzi wa anthu oononga?" 92. "Lero, Ife
tidzasunga thupi lako, kuti ukhale chizindikiro kwa onse
amene adza m'mbuyo mwako. Ndithudi anthu ambiri ndi
oiwala zizindikiro zathu."
93. Ndithudi Ife tidawakhazika ana a Israyeli malo abwino
ndipo tidawapatsa zinthu zabwino. Ndipo iwo sadatsutsane
mpaka pamene nzeru zinadza kwa iwo. Ndithudi Ambuye
wako adzaweruza pakati pawo pa zinthu zimene amasiyana
pa tsiku la kuuka kwa akufa.
94. Ngati ukaika pa zimene tavumbulutsa kwa iwe,
afunse iwo amene adawerenga Buku la kale iwe usanadze.
Ndithudi, choonadi chadza kwa iwe kuchokera kwa
Ambuye wako kotero usakhale mmodzi wa okaika. 95. Ndipo
usakhale mmodzi wa anthu amene adakana chivumbulutso
cha Mulungu chifukwa ngati utero udzakhala mmodzi
olephera.
96. Ndithudi iwo amene Mau a Ambuye wawo
akwaniritsidwa, sadzakhulupirira. 97. Ngakhale atalandira
chizindikiro china chilichonse mpaka pamene adzaone
chilango chowawa. 98. Kodi padalinso mzinda wina
umene unakhulupirira ndipo kuti chikhulupiriro chake
chinaupulumutsa kupatula anthu a Yona, pamene iwo
adakhulupirira? Ife tidawachotsera chilango chochititsa

manyazi m'moyo uno ndi kuwalola kusangalala pa kanthawi
kochepa.
99. Ngati Ambuye wako akadafuna, anthu onse a pa
dziko lapansi akanakhulupirira mwa Iye yekha. Kodi iwe
ungakakamize anthu kuti akhale okhulupirira? 100. Palibe
munthu angakhulupirire pokhapokha m'chifuniro cha
Mulungu. Iye adzagwetsa mkwiyo wake pa anthu opanda
nzeru.
101. Nena, "Taonani zonse zimene zili kumwamba ndi pa
dziko lapansi!" Koma zizindikiro ndiponso anthu opereka
chenjezo, siaphindu kwa anthu osakhulupirira. 102. Kodi pali
chimene akudikira kupatula zimene zinaoneka m'masiku
a anthu omwe analipo iwo asanadze? Nena, "Dikirani,
ine ndili nanu ngati mmodzi mwa odikira." 103. Pambuyo
pake tinawapulumutsa Atumwi athu pamodzi ndi amene
amakhulupirira. Kotero ndi koyenera kwa Ife kupulumutsa
anthu okhulupirira.
104. Nena, "Oh inu anthu! Ngati inu muli ndi chikaiko pa
chipembedzo changa, dziwani kuti ine sindidzapembedza
zomwe mukuzipembedza kuonjezera pa Mulungu
weniweni. Koma ine ndikupembedza Mulungu amene
amakuphani nonse ndipo ndalamulidwa kuti ndikhale
mmodzi wa anthu okhulupirira." 105. Ine ndidalamulidwa
kuti, "Tsatira chipempedzo chopembedza Mulungu
mmodzi ndipo usakhale mmodzi mwa anthu opembedza
mafano." 106. Ndipo usapembedze wina aliyense yemwe
si Mulungu, amene sangathe kukuthandiza kapena
kukuononga chifukwa, utatero, udzakhala mmodzi wa
wochita zoipa. 107. Ngati Mulungu akupatsa mavuto palibe
wina amene angawachotse kupatula Iye yekha ndipo ngati

Iye akufunira zabwino, palibe wina amene angabweze zokoma zake zimene Iye amapereka kwa kapolo wake amene Iye wamufuna. Ndipo Iye ndi wokhululukira ndiponso Mwini chisoni chosatha.
108. Nena, “Oh inu anthu! Choonadi chadza kwa inu kuchokera kwa Ambuye wanu. Aliyense amene atsogozedwa atero podzithandiza iye mwini ndipo aliyense amene asochera adzisocheretsa yekha. Ine sindili wokusamalirani inu.” 109. Tsatira zimene zikuvumbulutsidwa kwa iwe ndipo pirira mpaka pamene Mulungu aweruza. Iye ndi Muweruzi wodziwa kuposa aweruzi ena onse.

Sura 11 • Hûd

# Hud

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. *Alif Lam Ra.*

Ndi Buku limene mavesi ake akonzedwa bwino. Ndipo adafotokozedwa mwatsatane tsatane kuchokera kwa Mwini nzeru ndi wodziwa. 2. Kuti musapembedze wina aliyense koma Mulungu. Ndithudi ine ndine wochokera kwa Iye wochenjeza ndi wobweretsa nkhani zabwino.
3. Ndikuti mupemphe chikhululukiro kwa Ambuye wanu ndipo lapani kwa Iye yekha kuti Iye akupatseni zinthu zabwino mpaka pa nthawi yoikidwa. Ndi kupereka kwa aliyense wochita zabwino chisomo chake chomuyenera. Ndipo ngati inu mukana, ine ndichita mantha ndi chilango

chimene chingadze pa inu patsiku lalikulu. 4. Ndi kwa
Mulungu kumene nonse mudzabwerera ndipo Iye ali ndi
mphamvu pa zinthu zonse. 5. Zoonadi! Iwo amakuta mitima
yawo kuti akhoza kubisala kwa Iye. Ndithudi ngakhale
pamene iwo avala zovala zawo, Iye amadziwa zonse zimene
akubisa ndi zimene akuulula. Iye amadziwa zonse zimene
zili m'mitima mwawo. 6. Ndipo palibe cholengedwa
padziko lapansi chimene chakudya chake sichichokera
kwa Mulungu. Ndipo Iye amadziwa malo ake okhala ndi
malo ake a mpumulo. Zonse zili m'Buku lofotokozera
bwino zinthu.

7. Iye ndi amene adalenga kumwamba ndi dziko lapansi
m'masiku asanu ndi limodzi ndipo Mpando wake udali
pamwamba pa madzi kuti akuyeseni kuti ndani wa inu
amene ali ndi ntchito zabwino. Ndipo iwe ukadanena kuti:
"Inu ndithudi mudzaukitsidwa pambuyo pa kufa," anthu
osakhulupirira akadanena kuti: "Ichi si china chilichonse
koma matsenga enieni." 8. Ndipo ngati Ife titachedwetsa
chilango chawo mpaka pa tsiku lokhazikitsidwa, iwo
adzafunsa kuti: "Nanga ndi chifukwa chiyani tsikulo lili
kuchedwa?" Ndithudi pa tsiku limene izi zidzachitika,
palibe chilichonse chimene chingadzapirikitse chilangocho
ndipo zoopsa zimene iwo ali kuseka zidzawazungulira iwo
onse.

9. Ndipo ngati Ife timulawitsa munthu chifundo chathu
kenaka ndi kumulanda, ndithudi, iye amadandaula
ndiponso amakhala osuliza. 10. Koma ngati Ife titamuonetsa
munthu chisoni chathu, pambuyo pa mavuto amene
adapeza, iye adzati: "Mavuto atha kwa ine" Ndithudi iye
amakhala mosalabadira ndiponso modzikweza kwambiri.

11. Kupatula iwo amene amapirira ndi kuchita ntchito
zabwino. Iwo adzakhala ndi chikhululukiro ndi malipiro
akulu.
12. Mwina iwe ukhoza kusiya kunena zina za zimene
zavumbulutsidwa kwa iwe ndi kukhala ovutika mu mtima
chifukwa chakuti iwo amanena kuti, "Bwanji chuma
sichidatumizidwe kwa iye kapena bwanji Mngelo sadadze
pamodzi ndi iye?" Komatu iwe ndiwe wochenjeza. Ndipo
Mulungu ndiye Msungi wa zinthu zonse. 13. Kapena iwo
akunena kuti: "Iye wapeka yekha!" Nena, "Nanunso
bweretsani mitu khumi yofanana ndi yopekedwayi. Ndipo
itanani wina amene mungathe kumuitana kupatula Mulungu
ngati muli kunena zoona." 14. Akapanda kukuyankha, dziwa
kuti chivumbulutso chatumizidwa ndi nzeru ya Mulungu.
Ndipo kuti kulibe wina woti apembedzedwe kupatula Iye
yekha. Kodi tsopano mudzakhala ogonjera?
15. Aliyense amene afuna moyo wa m'dziko lino pamodzi
ndi zokondweretsa zake, Ife tidzawalipira molingana ndi
ntchito zawo , mopanda kuchotsera chilichonse. 16. Awa
ndiwo anthu amene sadzapeza chilichonse m'moyo umene
uli nkudza kupatula moto ndipo zonse zimene amachita
pa dziko lapansi zidzaonongeka ndiponso ntchito zawo
zimene ankachita zidzakhala zopanda pake.
17. Kodi iwo amene amadalira umboni wooneka
wochokera kwa Ambuye wawo, umene mboni yochokera
kwa Iye amautsatira, ndipo iwo usanadze, linadza Buku
la Mose, ulangizi ndi chisomo, iwo amakhulupirira koma
a mpatuko amene amalikana, kumoto ndiko kudzakhala
malo awo okumana. Motero iwe usakaike za ilo. Ndithudi

ndi choonadi chochokera kwa Ambuye wako koma anthu
ambiri sakhulupirira.
18. Kodi wolakwa kwambiri ndani kuposa munthu
amene amapeka bodza lokhudza Mulungu? Anthu otero
adzaonetsedwa pamaso pa Ambuye wawo ndipo mboni
zidzati: "Awa ndiwo amene anali kunamizira Ambuye
wawo." Mosakaika! Matemberero a Mulungu ali pa anthu
ochita zoipa. 19. Iwo amene amaletsa anzawo kuti asatsatire
njira ya Mulungu ndipo amafuna kuti njira ya Mulungu
ikhale yopindika ndiponso amakana kuti kuli moyo
wina umene uli nkudza. 20. Wotere sadzathawa padziko
lapansi ndiponso alibe owateteza kupatula Mulungu!
Chilango chawo chidzaonjezeredwa chifukwa chakuti
iwo samafuna kumva ndiponso samaona. 21. Awa ndiwo
amene ataya mizimu yawo ndipo zinthu zawo zonse
zabodza zidzawathawira. 22. Ndithudi iwo ndiwo amene
sadzapindula zambiri mmoyo umene uli nkudza.
23. Ndithudi iwo amene akhulupirira ndipo amachita
ntchito zabwino, ndipo amadzichepetsa kwambiri pamaso
pa Ambuye wawo, iwo adzakhala eni ake a Paradiso
ndipo kumeneko adzakhalako mpaka kalekale. 24. Fanizo
la magulu awiri a anthu lili ngati munthu wakhungu ndi
wosamva, wopenya ndi wakumva. Kodi magulu awiriwa ndi
ofanana? Kodi simungaganize pamenepa?
25. Zoonadi tidamutumiza Nowa kwa anthu ake nati:
"Ndithudi ine ndine mchenjezi wanu weniweni. 26. Kuti
musapembedze wina aliyense koma Mulungu, ndithudi,
ine ndili kukuderani nkhawa pa chilango cha tsiku
lowawa." 27. Akuluakulu osakhulupirira amene adali pakati
pa anthu ake adati: "Ife tili kukuona iwe ngati munthu

onga ife tomwe ndiponso tili kuona kuti onse amene ali kukutsatira kuti ndi anthu apansi kwambiri pakati pathu ndiponso iwo akutsatira iwe osaganiza. Ndipo ife sitili kuona china chilichonse mwa iwe chopambana ife ndipo, kunena moona, tikuganiza kuti inu ndinu abodza.”

28. Iye adati: “Oh inu anthu anga! Mukuona bwanji? Ngati ine ndili ndi umboni wochokera kwa Ambuye wanga ndiponso wandipatsa chifundo kuchokera kwa Iye, ndipo umboniwo wabisika kwa inu. Kodi ife tingakuumirizeni kuti mumvomere pamene mukunyansidwa nawo?” 29. “Oh inu anthu anga! Ine sindikukupemphani chuma chifukwa cha ichi, malipiro anga sali kwa wina koma Mulungu yekha. Ndipo ine sindiwathamangitsa amene akhulupirira. Ndithudi, iwo adzakumana ndi Ambuye wawo. Koma ine ndikukuonani kuti ndinu anthu osadziwa.” 30. “Oh inu anthu anga! Ndani anganditeteze ine kwa Mulungu ngati nditawapitikitsa iwo? Kodi inu simungaganizire pamenepa?” 31. “Ine sindili kunena kwa inu kuti ndili ndi Nkhokwe za chuma cha Mulungu kapena kuti ndimadziwa zinthu zobisika. Ine sindili kunena kuti ndine Mngelo ayi ndiponso ine sindinena za iwo amene maso anu akuwanyoza kuti Mulungu sadzawapatsa zokoma zake. Mulungu amadziwa bwinobwino zonse zimene zili m’mitima mwawo, chifukwa nditatero, ndithudi, ine ndidzakhala m’modzi wa anthu olakwa.”

32. Iwo anati, “Iwe Nowa! Iwe watsutsana nafe kwambiri. Tsopano bweretsa msangamsanga chilango chimene uli nkutiopsyeza nacho ngati uli mmodzi wa anthu onena zoona!” 33. Iye adati, “Mulungu yekha adzakubweretserani chilango chake pamene Iye afuna. Ndipo inu simudzathawa

ai.” 34. “Ndiponso ulangizi wanga siudzakuthandizani
ngakhale nditafuna kukulangizani ngati chifuniro cha
Mulungu ndi kukusocheretsani. Iye ndi Ambuye wanu
ndipo ndi kwa Iye mudzabwerera.”
35. Kapena iwo akunena kuti, “Iye wapeka.” Nena, “Ngati
ine ndapeka, tchimo ndi langa koma ine ndili nazo kutali
zoipa zimene mukuchita.”
36. Ndipo Mau a Mulungu adavumbulutsidwa kwa Nowa
ponena kuti: “Palibe mmodzi mwa anthu ako amene
adzakhulupirira kupatula okhawo amene akhulupirira
kale. Motero usamve chisoni chifukwa cha zimene
anali kuchita.” 37. “Ndipo panga chombo pamaso pathu
ndi chilamulo chathu ndipo usalankhule mmalo mwa
anthu ochimwa. Ndithudi onse adzamizidwa m’madzi.”
38. Pamene iye adayamba kupanga chombo, ndipo nthawi
zonse pamene akuluakulu a anthu ake anali kudutsa
pafupi ndi iye, iwo amamuchita chipongwe. Iye adati:
“Ngati mukutichita chipongwe, nafenso tidzakubwezerani
chipongwe monga mmene mukutichitira ife.” 39. “Ndipo
inu mudzadziwa posachedwa yemwe chilango chochititsa
manyazi chidzamfikira, ndiponso iwo amene adzalandira
chilango chosatha.”
40. Kufikira pamene chilamulo chathu chidadza,
ndipo nthaka idayamba kutulutsa madzi. Ife tinati:
“Lowetsa m’chombo zinthu ziwiriziwiri, (chachimuna
ndi chachikazi), anthu a banja lako kupatula iye amene
chiweruzo chaperekedwa kale ndi iwo amene akhulupilira.
Koma si ambiri amene adali okhulupirira ndi iye kupatula
ochepa okha. 41. Iye adati, “Kwerani m’menemo, M’dzina la
Mulungu chidzayenda mnjira yake ndipo chidzaima pamalo

pofunikira. Ndithudi Ambuye wanga ndi wokhululukira
ndipo ndi wachisoni chosatha.” 42. Motere icho chinayenda
pa mafunde okhala ngati mapiri, ndipo Nowa adamuitana
mwana wake amene adaima pambali. “Oh mwana wanga!
Kwera chombo pamodzi ndi ife ndipo usakhale pamodzi ndi
anthu osakhulupirira.” 43. Iye adati: “Ine ndidzathawira ku
phiri limene lidzanditeteza ku chigumula cha madzi.” Nowa
adati, “Lero palibe woteteza wina ku lamulo la Mulungu
kupatula yekhayo amene Mulungu adzamuonetsera
chisomo chake.” Ndipo funde lidatchinga pakati pawo
ndipo mwana wa Nowa anali mmodzi wa omizidwa.
44. Ndipo kudanenedwa: “Nthaka meza madzi ako! Ndi
kumwamba siya kugwetsa mvula.” Chigumula chinasiya
ndipo chifuniro cha Mulungu chinakwaniritsidwa. Ndipo
chombo chinadzaima pa phiri la Al Judi ndipo panamveka
mawu onena kuti: “Chionongeko chili kwa anthu ochita
zoipa.”
45. Ndipo Nowa adaitana kwa Ambuye wake nati:
“Ambuye! Ndithudi mwana wanga ndi mmodzi wa anthu
a banja langa. Lonjezo lanu, ndithudi, ndi loona. Inu ndinu
oweruza bwino kuposa oweruza onse.” 46. Mulungu adati:
“Iwe Nowa! Ndithudi iye si wabanja lako ayi. Ndithudi
ntchito zake si zabwino motero usandifunse zinthu zimene
iwe siudziwa. Ndili kukuchenjeza kuti usakhale mugulu
la mbuli ayi.” 47. Nowa adati: “Ine ndipempha chitetezo
chanu, Ambuye, chifukwa chokupemphani zinthu zimene
ine sindili kuzidziwa. Ndipo Inu ngati simundikhululukira
ndi kundimvera ine chisoni, ndithudi, ine ndidzakhala
mmodzi wa anthu olephera.”
48. Kudanenedwa: “Iwe Nowa! Tsika pa mtunda ndi

mtendere wochokera kwa Ife ndi madalitso akhale kwa
iwe ndi kugulu la anthu amene ali nawe, koma anthu onse
tidzawasangalatsa pa kanthawi ndipo pambuyo pake
chidzawapezanso chilango chowawa chochokera kwa Ife."
49. Zimenezi ndi nkhani zobisika zimene tikuvumbulutsa
kwa iwe, zimene iwe kapena anthu ako samazidziwa
chisanabwere chivumbulutso ichi. Motero pirira. Ndithudi
mapeto abwino ndi a iwo amene amuopa Mulungu.
50. Ndipo kwa mtundu wa Aad, tidatumiza m'bale wawo
Hud. Iye adati: "Oh anthu anga! Pembedzani Mulungu.
Inu mulibe mulungu wina kupatula Iye yekha. Ndithudi
inu simuchita china chili chonse koma kupeka bodza
basi." 51. "Oh anthu anga! Ine sindikukupemphani malipiro
pazimenezi. Malipiro anga sali ndi wina koma ali ndi Iye
amene adandilenga. Kodi simutha kumva zimenezi?" 52. "Oh
Anthu anga! Mpempheni Ambuye wanu chikhululukiro
ndipo lapani kwa Iye chifukwa Iye adzakutumizirani mvula
yambiri ndipo adzakuonjezerani mphamvu pamwamba pa
mphamvu zanu. Kotero musatembenuke kukhala anthu
oipa."
53. Iwo adati, "Oh iwe Hud! Iwe siunatibweretsere umboni
wokwana. Ndipo ife sitidzasiya kupembedza milungu
yathu chifukwa cha mawu ako! Ndipo ife sitikukhulupirira
iwe ayi." 54. "Zimene tilikunena ndizakuti ina ya milungu
yathu yakupatsa iwe tsoka." Iye adati: "Ndithudi Mulungu
ndiye mboni yanga ndipo nanunso chitirani umboni
kuti ine ndatalikirana nazo zimene mukamapembedza
mulikuonjezera." 55. "Motero nonsenu konzani chiwembu
chanu pa ine ndipo musandichedwetse." 56. "Ine ndaika
chikhulupiliro changa mwa Mulungu, Ambuye wanga

ndiponso Ambuye wanu. Palibe chinthu cha moyo pa
dziko lapansi chimene tsogolo lake sililamulidwa ndi Iye.
Ndithudi Ambuye wanga ndi amene ali pa njira yoyenera."
57. "Ndipo ngati mutembenuka, ine ndakuuzani Uthenga
umene ndatumizidwa kwa inu. Ambuye wanga adzaika,
m'malo mwanu, anthu ena ndipo inu simungamuchite
chinthu choipa chilichonse. Ndithudi Ambuye wanga ndi
Msungi wa zinthu zonse." 58. Ndipo pamene chiweruzo
chathu chidadza, Ife tidamupulumutsa Hud, kudzera
mu Chisomo chathu, pamodzi ndi amene adakhulupirira
ndi iye. Ife tidawapulumutsa ku chilango chokhwima.
59. Amenewa anali anthu a Aad. Iwo adakana Mawu a
Ambuye wawo, ndipo adanyoza Atumwi ake ndipo
anatsata malamulo a atsogoleri awo a nkhanza ndi okana
chilungamo. 60. Ndipo iwo adatsatiridwa ndi temberero
m'dziko lino ndipo adzakhala otembereredwa pa tsiku la
chiweruzo. Mosakaika, ndithudi, anthu a Ad adamukana
Ambuye wawo. Motero tinathana nawo Ad, anthu a Hud.
61. Ndipo kwa Thamoud, tidatumiza m'bale wawo Saleh.
Iye adati: "Oh anthu anga! Mpembedzeni Mulungu,
chifukwa inu mulibe mulungu wina kupatula Iye yekha.
Iye ndiye amene adakulengani inu kuchokera ku nthaka,
ndipo adakupatsani inu malo okhala pa nthakayo. Motero
funani chikhululukiro kwa Iye ndipo idzani kwa Iye ndi
kulapa. Ndithudi Ambuye wanga ali pafupi nanu ndipo
Iye adzamva mapemphero anu." 62. Iwo adati: "Iwe
Saleh! Ndithudi iwe wakhala pakati pathu ndipo udali
chiyembekezo chathu. Kodi iwe utiletsa kupembedza
zimene amapembedza makolo athu? Ndithudi ife tili
ndi chikaiko chambiri ndi chipembedzo chimene uli

kutiitanira.” 63. Iye adati: “Oh anthu anga! Ndiuzeni ngati ine ndili ndi umboni wokwanira wochokera kwa Ambuye wanga ndipo Iye wandipatsa chisomo kuchokera kwa Iye, ndani angandipulumutse ine kuchokera ku chilango cha Mulungu ngati nditamunyoza? Inu simungaonjezere china chilichonse kwa ine koma kutayika.”

64. “Oh Anthu anga! Iyi ndi Ngamira yaikazi, mwini wake ndi Mulungu, ndipo ndi chizindikiro chooneka kwa inu. Isiyeni kuti izidya mwachifuniro cha Mulungu m’dziko lake ndipo musaizunze chifukwa chilango chingadze pa inu mwamsanga.” 65. Koma iwo adaipha ngamirayo ndipo iye adati: “Inu basangalalani m’nyumba zanu masiku atatu. Chimenecho ndi chipangano chimene sichili chabodza.” 66. Ndipo pamene chiweruzo chathu chimadza, Ife tinamupulumutsa Saleh pamodzi ndi amene adakhulupirira ndi iye kudzera m’Chisomo chathu, kuchokera m’masautso a tsiku limeneli. Ndithudi Ambuye wako ndi wanyonga, ndi wopambana. 67. Ndipo mkuwo wowopsa udawaononga anthu ochita zoipa ndipo anthu onse adali lambilambi m’nyumba zawo atafa. 68. Kukhala ngati sadakhalepo pa malo amenewo. Mosakaika, ndithudi, a Thamoud sadakhulupirire mwa Ambuye wawo. Motero anatha anthu a Thamoud.

69. Ndithudi Atumwi athu adadza kwa Abrahamu ndi nkhani yabwino. Iwo adati: “Mtendere!” Iye anayankha: “Mtendere” ndipo posakhalitsa iye adabweretsa nyama ya ng’ombe yowotcha. 70. Ndipo pamene iye adaona kuti manja awo sakukhudza nyamayo adawadabwa, nachita mantha. Iwo adati: “Usaope. Ife tatumidwa kwa anthu a Loti.” 71. Ndipo mkazi wake adali chiimire pompo, naseka.

Ife tidamuuza kuti adzabereka Isake ndipo kuti Isake
adzabala Yakobo. 72. Iye adati: "Kalanga ine! Kodi ine
ndingabereke pamene ndine wokalamba ndipo mwamuna
wanga ndi wokalambanso? Ndithudi ichi ndi chinthu
chododometsa." 73. Iwo adati: "Kodi iwe uli kuwadabwa
malamulo a Mulungu? Madalitso ndi chisomo cha Mulungu
chikhale pa inu a m'banja la Abrahamu. Ndithudi Iye ndi
wotamandidwa ndiponso wolemekezeka."
74. Ndipo pamene Abrahamu adamuchoka mantha ndi
kumfikira nkhani yabwino, iye adatifunsa Ife za anthu a Loti.
75. Ndithudi Abrahamu anali woleza mtima, wodzichepetsa
ndiponso munthu wodzipereka kwa Mulungu. 76. Angelo
adati: "Iwe Abrahamu! Siya zimenezo. Ndithudi lamulo la
Ambuye wako ladza. Ndithudi kudzadza chilango kwa iwo
chimene sichingaletsedwe."
77. Ndipo pamene Atumwi athu adadza kwa Loti, iye adali
wodandaula kwambiri ndi kubanika mumtima chifukwa
cha iwo. Ndipo adati: "Ndithudi ili ndi tsiku loopsa."
78. Anthu ake adadza kwa iye akuthamanga ndipo pambuyo
adali kuchita zinthu zoipa. Iye adati: "Oh! Anthu anga,
awa ndi ana anga akazi, amene ali oyera kwa inu. Opani
Mulungu ndipo musandiyalutse kwa alendo anga. Kodi
palibe pakati panu munthu mmodzi wangwiro?" 79. Iwo
adati: "Iwe ukudziwa kuti tilibe khumbo mu ana ako akazi
ayi. Ndiponso iwe ukudziwa zimene tikufuna."
80. Iye adati: "Ine ndikadakhala ndi mphamvu zoti
ndikugonjetseni kapena ndikanapeza munthu wina
wamphamvu zambiri ndikadamenyana nanu." 81. Iwo adati:
"Iwe Loti! Ndithudi ife ndife Atumwi Ambuye wako,
iwo sakukhudza, choka pamodzi ndi anthu ako pakati pa

usiku. Ndipo usalole wina wa inu kuti ayang'ane m'mbuyo kupatula mkazi wako, ndithudi, adzaona zonse zimene ena adzaone. Ndithudi lonjezo lawo ndi m'mamawa. Kodi m'mawa si pafupi?" 82. Ndipo pamene chilamulo chathu chidadza, Ife tidatembenuza pamwamba pa Mzinda kukhala pansi ndipo tidagwetsa pa iwo miyala youmbidwa ndi nthaka ya makande younjikika. 83. Yokhala ndi zizindikiro, yochokera kwa Ambuye wako ndipo iyo siili kutali ndi anthu wosalungama.

84. Ndipo kwa anthu a ku Midiyani tidawatumizira m'bale wawo Shoaib. Iye adati: "Oh Anthu anga! Pembedzani Mulungu, chifukwa inu mulibe mulungu wina koma Mulungu mmodzi yekha ndipo musapungule miyeso ya zinthu. Ine ndikuona kuti inu ndinu anthu a chuma. Ine, ndithudi, ndili kuchita mantha ndi chilango cha tsiku limene lidzakuzungulirani inu." 85. "Anthu anga! Kwaniritsani muyeso wa zinthu ndipo yesani mwachilungamo ndipo musawapungulire anthu katundu wawo ndipo musachite zoipa padziko ndikuyambitsa chisokonezo." 86. "Zimene Mulungu wakusiyirani inu ndi zimene zili zabwino kwa inu ngati muli okhulupirira. Ndipo ine sindine wokuyang'anirani ayi."

87. Iwo adati: "Iwe Shoaib! Kodi mapemphero ako akulamulira kuti ife tiyenera kuleka kupembedza milungu ya makolo athu kapena kuti sitiyenera kuchita zimene tifuna ndi chuma chathu? Ndithudi iwe ndiwe wopirira ndiponso wa nzeru zokhazikika."

88. Iye adati: "Ndiuzeni! Ngati ine ndili ndi umboni woonekera wochokera kwa Ambuye wanga ndipo Iye wandipatsa gawo labwino. Ine sindifuna kusemphana

nanu pochita chinthu chimene ndili kukuletsani. Palibe chilichonse chimene ndifuna koma kukonza mmene ndingathere. Ndipo ulangizi wanga siubwera kuchokera kwa wina aliyense kupatula Mulungu. Mwa Iye ndaika chikhulupiriro changa ndipo kwa Iye ndiko ndimalapa." 89. "Oh anthu anga! Musalole kuti kusagwirizana kwanu ndi ine kuti kubweretse pa inu mavuto amene adadza pa anthu a Nowa, kapena pa anthu a Hud ndi Saleh ndiponso sikale pamene anthu a Loti adaonongeka." 90. "Ndipo funani chikhululukiro cha Ambuye wanu, ndiponso lapani kwa Iye. Ndithudi Ambuye wanga ndi wa Chisoni ndiponso wa Chikondi chosatha."

91. Iwo adati: "Oh Shoaib! Zambiri zimene unena ife sitili kuzizindikira ndipo ife tili kuona kuti ulibe mphamvu pakati pathu. Pakadapanda mtundu wako, ndithudi, ife tikadakuponya miyala ndiponso iwe ulibe mphamvu zoposa zathu." 92. Iye adati: "Oh anthu anga! Kodi mtundu wanga ndi olemekezeka kwambiri kuposa Mulungu? Ndipo inu mwamuponya Iye kumbuyo kwanu? Ndithudi Ambuye wanga ndi wodziwa zonse zimene muchita." 93. "Oh anthu anga! Chitani chimene mufuna kuti muchite, nanenso ndidzachita zanga. Inu mudzadziwa kuti ndani adzalangidwa ndi chilango chochititsa manyazi ndiponso kuti kodi ndani amene ali kunama! Ndithudi dikirani nanenso ndili kudikira pamodzi ndi inu."

94. Ndipo pamene lamulo lathu lidadza tidamupulumutsa Shoaib, pamodzi ndi anzake onse amene anali wokhulupirira mwa chisomo chathu. Ndipo mkuwo waukulu udawaononga anthu onse ochita zoipa ndipo onse adali lambilambi m'nyumba zawo. 95. Kukhala ngati

iwo sadakhalemo m'menemo! Motero adaonongeka anthu
a ku Midiyani monga momwe adaonongekera anthu a ku
Thamoud.
96. Zoonadi tidamutumiza Mose ndi zizindikiro zathu
ndiponso umboni wooneka. 97. Kwa Farao ndi nduna zake,
iwo anatsatira malamulo a Farao ndipo malamulo a Farao
sanali olungama. 98. Iye adzawatsogolera anthu ake pa tsiku
la chiweruzo ndipo adzawalowetsa ku moto. Aipirenji
malo omwe adatengedwerako. 99. Ndipo anatsatiridwa
ndi matemberero m'moyo wa m'dziko lino ndi patsiku la
chiweruzo. Iyipirenji mphotho yomwe adzapatsidwe.
100. Iyi ndi nkhani, ya m'mizinda imene tinaononga ndipo
tili kukufotokozera iwe, ndipo ina mwa Mizindayo ilipo
pamene ina idaonongeka. 101. Ife sitinawapondereze ayi
koma adadzipondereza okha. Motero milungu yawo imene
anali kuipembedza kuonjezera pa Mulungu siidawathandize
chilichonse pamene chiweruzo cha Ambuye wako chidadza
ndiponso milungu yawo sidawaonjezere kalikonse koma
chionongeko.
102. Chimenecho ndicho chilango cha Ambuye wako
akafuna kulanga mzinda wa anthu ochita zoipa. Ndithudi
chilango chake ndi chokhwima ndi chowawa kwambiri.
103. Ndithudi mu izo muli chizindikiro kwa iye amene
aopa chilango cha moyo umene uli nkudza. Ndi tsiku
limene anthu onse adzasonkhanitsidwa pamodzi ndiponso
ili ndi tsiku lomwe chilichonse chidzakhalapo. 104. Ife
tili kulichedwetsa mpaka pa nthawi yokhazikitsidwa.
105. Ndipo pamene tsikuli lidza, palibe munthu amene
adzalankhula opanda chilolezo cha Mulungu. Ena a iwo
adzakhala a tsoka pamene ena adzakhala amwayi.

106. Akhala iwo amene adzakhala a tsoka, iwo akakhala
m'moto ali kubuula mokweza ndiponso motsitsa. 107. Iwo
adzakhala komweko mpaka pamene kumwamba ndi dziko
lapansi zidzakhale zilipobe kupatula ngati Ambuye wako
afuna kusintha. Ndithudi Ambuye wako amachita zimene
afuna. 108. Akakhala anthu odala, iwo adzakhala ku Paradiso
mpaka pamene kumwamba ndi dziko lapansi zidzakhale
zilipobe kupatula ngati Ambuye wako afuna kusintha,
mphatso yosatha mpaka kalekale. 109. Motero usakaike pa
zimene anthu awa apembedza. Iwo sali kupembedza koma
kungotsatira mmene makolo awo amapembedzera kale.
Ndipo ndithudi Ife tidzawalipira malipiro awo mopanda
kuchepetsa.

110. Ndithudi Ife tidamupatsa Mose Buku koma
mikangano inabuka pakati pawo ndipo kukadapanda kuti
liwu lochokera kwa Ambuye wako lidatsogola kale, lamulo
likadadza pa iwo. Ndithudi iwo ndi okaika kwambiri za
ili. 111. Ndithudi Ambuye wako adzalipira anthu molingana
ndi ntchito zawo. Ndithudi Iye amadziwa zonse zimene
akuchita.

112. Motero pitiriza kukhala m'njira yoyenera monga
momwe walamulidwira pamodzi ndi onse amene alapa
pamodzi ndi iwe ndipo usapyole malire. Ndithudi Iye
amaona zonse zimene mumachita. 113. Ndipo usatsatire
anthu ochita zoipa chifukwa moto ungakupezeni ndiponso
palibe wina wokuthandizani kupatula Mulungu ndiponso
palibe wokuthandizani. 114. Ndipo chita mapemphero
ako nthawi ziwiri za masana ndi m'maola oyambirira a
usiku. Ndithudi ntchito zabwino zimafafaniza machimo.
Chimenechi ndi chikumbutso kwa anthu okumbukira.

115. Kotero pirira. Ndithudi Mulungu sasokoneza mphotho
ya ochita zabwino.

116. Kukadakhala kuti pakati pa mibadwo imene
inalipo kale, panali anthu a nzeru oletsa anthu kuchita
zoipa padziko lapansi kupatula owerengeka amene Ife
tidawapulumutsa pakati pawo. Iwo amene amachita
zoipa anali kutsatira zokoma za m'moyo uno ndipo adali
kupitiliza kuchita zoipa. 117. Ndipo sizinali koyenera kuti
Ambuye wako aononge mizinda mwankhanza pamene
anthu ake anali kuchita zabwino.

118. Ndipo Ambuye wako akadafuna, ndithudi,
akadawapanga anthu onse kukhala a chipembedzo
chimodzi koma akadapitiriza kukhala osiyana. 119. Kupatula
yekhayo amene Ambuye wako wamuonetsera chisomo
chake ndipo ndicho chifukwa chake chimene Mulungu
adawalengera. Mawu a Ambuye wako adzakwaniritsidwa
"Ndithudi Ine ndidzadzadza Gahena ndi Majini ndi anthu
onse pamodzi."

120. Ndipo zonse zimene tili kukuuza iwe za nkhani za
Atumwi ndi kulimbikitsa mtima wako. Kudzera mu izi
choonadi ndi ulangizi wadza kwa iwe ndiponso uthenga
wa chikumbutso kwa anthu okhulupirira. 121. Auze anthu
osakhulupirira kuti: "Chitani mmene mungathere, nafenso
tidzachita chimodzimodzi." 122. Dikirani! Ndithudi
nafenso tili kudikira. 123. Zobisika zonse zimene zili
kumwamba ndi pa dziko lapansi ndi za Mulungu ndipo
zonse zimabwerera kwa Iye. Motero mpembedzeni Iye
ndipo ika chikhulupiriro chako mwa Iye. Ambuye wako
saiwala zimene mukuchita.

# YUSUF

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. *Alif Lam Ra.*

Awa ndi mawu a Buku lofotokoza bwino. 2. Ndithudi Ife
talivumbulutsa ilo ngati Korani ya Chiarabu kuti mukhale
ozindikira. 3. Ife tili kukuuza iwe nkhani zabwino kudzera
m'Korani ino. Ndipo isanafike iwe udali m'gulu la anthu
amene samadziwa za ilo.
4. Pamene Yosefe adawauza abambo ake kuti, "Oh abambo
anga! Ndithudi ine ndaona nyenyezi khumi ndi imodzi
ndiponso dzuwa ndi mwezi zonsezi zili kundigwadira ine."
5. Iye adati, "Oh Mwana wanga! Usauze wina aliyense wa
abale ako za maloto ako, chifukwa mwina akhoza kukonza
chiwembu choti akuononge iwe. Ndithudi! Satana, kwa
munthu, ndi mdani woonekeratu." 6. "Kotero Ambuye
wako adzakusankha iwe ndikukuphunzitsa kutathauzira
maloto ndi kukwaniritsa chisomo chake pa iwe ndiponso
kwa ana a Yakobo, monga momwe adakwaniritsira kwa
makolo ako Abrahamu ndi Isake kale! Ndithudi Ambuye
wako ndi wodziwa zilizonse ndi Wanzeru."
7. Ndithudi m'mbiri ya Yosefe ndi abale ake muli
zizindikiro ndiponso phunziro kwa anthu ofuna kudziwa.
8. Pamene iwo adati, "Yosefe pamodzi ndi m'bale wake
amakondedwa kwambiri ndi abambo athu kuposa ife tonse
pamene ife tili gulu lamphamvu. Ndithudi, abambo athu

ali kulakwa koonekeratu.” 9. “Mumuphe Yosefe kapena
mukamutaye ku dziko lakutali kuti chikondi cha bambo
anu chikhale pa inu nokha ndipo pambuyo pa izi inu
mudzakhale anthu abwino.” 10. Mmodzi mwa iwo adati,
“Musamuphe Yosefe ayi koma ngati mufuna kuchita
china chake kamuponyeni m’chitsime chakuya chamdima
kapena anthu apaulendo adzamutola iye ngati mungathe
kutero.”

11. Iwo adati, “Abambo athu! Kodi chifukwa chiyani inu
simutikhulupirira ndi Yosefe pamene ife timamufunira
iye zabwino?” 12. “Mtumizeni iye pamodzi ndi ife
mawa kuti akasangalale ndi kusewera ndipo, ndithudi,
Ife tidzamusamalira iye.” 13. Iye adati, “Ndithudi
zikundidandaulitsa ine kuti mupite naye. Ine ndikuopa
kuti mmbulu ukhoza kukamudya iye inu mutamuiwala
iye.” 14. Iwo adati, “Ngati mmbulu ungamudye pamene ife
tili gulu lamphamvu, ndiye kuti tidzakhala olephera.”

15. Ndipo pamene iwo adapita naye, iwo adagwirizana
zomuponya m’chitsime chamdima ndipo Ife tidamuuza
iye kuti, “Iwe udzawauza zonsezi nthawi ina pamene iwo
sakudziwa.” 16. Ndipo iwo adabwera kwa abambo awo
ali kulira nthawi ya madzulo. 17. Iwo adati, “Oh bambo
wathu! Ife tinapita kukathamangitsana ndipo tinamusiya
Yosefe pa katundu wathu ndipo mmbulu wamudya iye,
koma inu simutikhulupirira ayi ngakhale kuti ife tili
kunena choonadi.” 18. Ndipo iwo adabweretsa malaya ake
ali ndi magazi omwe sanali a Yosefe. Iye adati, “Iyayi! Inu
mwapeka nokha nkhani koma kupirira ndi kwabwino. Ndi
Mulungu yekha amene ayenera kupemphedwa chithandizo
choteteza zimene mukunena.”

19. Ndipo gulu la anthu a paulendo lidabwera ndipo
lidatumiza mmodzi wa anthu otunga madzi, ndipo
adaponya ndowa yake, Iye adafuula nati, “Imvani nkhani
yabwino! Uyu mnyamata.” Ndipo iwo adamutenga iye
namubisa iye ngati katundu wawo wa malonda. Koma
Mulungu anali kudziwa zonse zimene iwo anali kuchita.
20. Ndipo iwo adamugulitsa pa mtengo wotsika wa ndalama
zowerengeka za siliva. Iwo sanalabadire china chilichonse
cha iye.
21. Ndipo munthu wa mtundu wa Aiguputo, amene
adamugula iye, adati kwa mkazi wake, “Mupatseni
malo aulemu mwina angatithandize kapena tikhoza
kumutenga kuti akhale mwana wathu.” Chomwecho Ife
tidamukhazikitsira malo okhala Yosefe, kuti timuphunzitse
kutanthauzira maloto. Ndipo Mulungu ali ndi mphamvu
ndi ulamuliro pa zinthu zake, koma anthu ambiri sadziwa.
22. Ndipo pamene iye adakula, tidamupatsa luntha ndi
nzeru. Chomwecho timalipira anthu ochita zabwino.
23. Ndipo mkazi wam’nyumba imene Yosefe anali
kukhala adamunyengerera kuti agone naye, ndipo adatseka
zitseko ndipo adati kwa iye, “Bwera kuno iwe.” Iye adati,
“Ndilikupempha chitetezo kwa Mulungu! Ndithudi
iye ndi bwana wanga amene amandisamalira bwino.
Ndithudi ochita zoipa sapambana ayi.” 24. Ndithudi mkazi
adamufunitsitsa Yosefe ndipo nayenso akadamufuna iye
pakadapanda kuti adaona umboni wochokera kwa Ambuye
ake. Ife tidatero ndi cholinga chomuteteza ku chinthu
chochititsa manyazi ndiponso choipa. Ndithudi iye adali
mmodzi wa akapolo athu otsogozedwa.
25. Ndipo onse adathamangitsana mpaka ku khomo ndipo

mkazi uja adamung'ambira Yosefe malaya ake kumbuyo.
Ndipo onse atafika pa khomo, adakumana ndi mwamuna
wake wa mkaziyo. Mkazi adati, "Kodi ndi malipilo otani
amene angaperekedwe kwa iye amene amafuna kuchita
zoipa mkazi wako kupatula kumangidwa kapena chilango
chowawa kwambiri? 26. Yosefe adati, "Si ndine koma mkaziyu
ndiye amene amandifuna ine." Ndipo munthu wina,
wachibale ndi mkaziyo, adaikira umboni nati, "Ngati malaya
ake ang'ambika kumimba ndiye kuti mkaziyu ali kunena
zoona, ndipo kuti iye ndi wabodza." 27. "Koma ngati malaya
ake ang'ambika kumbuyo, ndiye kuti mkaziyu wanama ndi
kuti iye ali kunena zoona." 28. Ndipo pamene mwamuna
wake adaona kuti malaya ake adang'ambika kumbuyo,
iye adati, "Ichi ndi chimodzi cha ukamberembere wanu
wa amayi. Ndithudi ukamberembere wanu ndi waukulu."
29. "Oh Yosefe! Usayankhulenso china chilichonse pankhani
izi. Iwe mkazi pempha chikhululukiro cha machimo ako.
Ndithudi iwe ndiwe mmodzi wa olakwa zedi."

30. Ndipo amai a mumzinda muja adati: "Mkazi wa
Mfumu alikunyenga mnyamata wake. Ndithudi iye anali
kumulakalaka zedi. Ndithudi ife tili kuona kuti mkaziyu
wasochera kwambiri." 31. Ndipo pamene iye adamva
zokamba zawo, adawatumizira uthenga owaitana ndi
kuwakonzera chakudya ndipo kwa aliyense, adamupatsa
mpeni wodyera. Ndipo adati kwa Yosefe, "Tulukira
kumene kuli iwo." Ndipo pamene iwo adamuona iye, onse
adamulemekeza ndipo adadzicheka manja awo. Ndipo iwo
adati, "Mulungu ayeretsedwe! Uyu si munthu ayi koma
mngelo wolemekezeka." 32. Mkazi uja adati, "Uyu ndiye
mnyamata uja amene nonsenu munali kundidzudzula naye.

Ndithudi ine ndidamunyenga koma iye adakanitsitsa.
Tsopano ngati iye sachita zimene ndikumulamulira,
ndithudi, adzaponyedwa ku ndende ndipo adzakhala
mmodzi wa anthu onyozedwa.” 33. Yosefe adati, “Oh Ambuye
wanga! Ndende ndi yabwino kwa ine kuposa zimene
akundiitanira. Ngati inu simunditchinjiriza kuchiwembu
chawo ine ndidzapendekera kwa iwo ndikukhala mmodzi
wa anthu osadziwa.” 34. Motero Ambuye wake adamva
pempho lake ndipo adam’phwetsera chiwembu chawo
pa iye. Ndithudi Iye amamva zonse ndipo amadziwa
chilichonse.
35. Ndipo zidaonekera kwa iwo, atatha kuona zizindikiro,
kuti iye am’mange mwakanthawi kochepa. 36. Ndipo
anyamata awiri adalowa m’ndende pamodzi ndi iye.
Mmodzi wa iwo adati, “Ndithudi ine ndalota ndili
kutcheza vinyo” Ndipo wina adanena kuti, “Ine ndinalota
nditanyamula pamutu panga mkate umene mbalame
zimadya. Tiuze matanthauzo ake. Ndithudi ife tikukuona
iwe kuti uli mmodzi wa anthu wochita zabwino.”
37. Yosefe adati, “Palibe chakudya chimene mumalandira,
ngati chakudya chanu, chimene chidze kwa inu ine
ndisanamasulire tanthauzo lake. Ichi ndicho chimene
Ambuye wanga adandiphunzitsa. Ndithudi ine ndasiya
chipembedzo cha anthu osakhulupirira mwa Mulungu
ndiponso m’moyo umene uli nkudza.” 38. “Ine ndidatsatira
chipembedzo cha makolo anga, Abrahamu, Isake ndi
Yakobo. Sikuli koyenera kwa ife kum’phatikiza Mulungu
ndi chilichonse. Ichi ndi chisomo cha Mulungu kwa ife ndi
kwa anthu a mitundu yonse, koma anthu ambiri sayamika
ayi.” 39. “Oh inu anzanga awiri a m’mndende! Kodi milungu

yosiyanasiyana ndi yabwino kapena wabwino ndi Mulungu
mmodzi yekha mwini mphamvu zonse?” 40. “Palibe chimene
mumapembedza kuonjezera pa Iye, koma mayina chabe
amene inu ndi makolo anu mudapeka, amene Mulungu
sadatumize umboni wa mayinawo. Chiweruzo chili
m’manja mwa Mulungu yekha. Iye adakulamulirani kuti
inu musamapembedze wina koma Iye yekha. Chimenecho
ndicho chipembedzo changwiro, koma anthu ambiri
sazindikira.”

41. “Oh inu akaidi anzanga awiri! Mmodzi wa inu
adzaperekera kwa Ambuye wake vinyo kuti amwe ndipo
wina adzapachikidwa pa mtanda ndipo mbalame zizidzadya
kuchokera pamutu pake. Motero lamulo laperekedwa pa
zinthu zimene munali kufunsa.” 42. Ndipo iye adati kwa
mmodzi amene iye adamuganizira kuti adzapulumuka,
“Ukandikumbukire ine kwa Ambuye wako.” Koma Satana
adamuiwalitsa kuti anene za Yosefe kwa Mfumu. Kotero
iye adakhala kundende zaka zingapo.

43. Ndipo Mfumu idati, “Ndithudi ine ndalota ndili
kuona ng’ombe zisanu ndi ziwiri zonenepa, zimene zinali
kudyedwa ndi ng’ombe zisanu ndi ziwiri zoonda ndiponso
ngala zina zisanu ndi ziwiri zaziwisi ndi ngala zisanu ndi
ziwiri zouma. Oh inu nduna zanga! Ndiuzeni tanthauzo la
maloto anga, ngati inu mungathe kutanthauzira maloto.”
44. Iwo adati, “Awa ndi maloto opanda ntchito ndipo ife
sititha kutanthauzira maloto.” 45. Ndipo munthu amene
adatulutsidwa m’ndende, adakumbukira patapita nthawi
yaitali ndipo adati, “Ine ndikuuzani kutanthauzira kwake
koma nditumizeni kuti ndipite.”

46. “Oh Yosefe munthu wa choonadi! Tiuzeni za ng’ombe

zisanu ndi ziwiri zonenepa zimene zinali kudyedwa ndi
ng'ombe zisanu ndi ziwiri zoonda ndiponso za ngala zisanu
ndi ziwiri zaziwisi ndi ngala zisanu ndi ziwiri zouma, kuti
ndibwerere ndikawauze anthu kuti akadziwe tanthauzo
lake?" 47. Yosefe adati, "Inu mudzabzala zaka zisanu
ndi ziwiri monga momwe mumachitira ndipo zimene
muzikolola muzizisiya mumakoko ake kupatula pang'ono
zomwe muzidya." 48. "Ndipo potha izi kudzadza zaka
zisanu ndi ziwiri za chilala pamene mudzadya zimene
mudasunga kupatula pang'ono zimene mudzasunge."
49. "Ndipo pambuyo pa izi kudzabwera chaka chimene
anthu adzalandira mvula yambiri, ndipo m'chaka
chimenecho azidzafinya zipatso."
50. Ndipo Mfumu idati, "Mubweretseni pamaso panga."
Koma pamene Kazembe wa Mfumu anadza kwa iye, Yosefe
adati, "Bwerera kwa Ambuye wako ndipo ukamufunse
za amayi amene adacheka manja awo. Ndithudi Ambuye
wanga adziwa za ukachenjede wawo." 51. Iyo inati, "Kodi
cholinga chanu chinali chotani pamene inu munali kufuna
kumunyenga Yosefe?" Amai anati, "Mulungu atiletse!
Ife sitidziwa choipa chilichonse chimene iye anachita."
Mkazi wa mfumu adati, "Tsopano choonadi chadziwika.
Ndine amene ndimamufuna ndipo iye, ndithudi, ndi
wachilungamo."
52. "Kuchokera mu izi bwana wanga adzadziwa kuti
sindidachite chinyengo pamene iye kunalibe ndiponso
kuti Mulungu satsogolera ntchito za anthu a chinyengo."
53. "Ine sindili kudziyeretsa, ndithudi, mtima wa munthu
umakonda zoipa kupatula pamene Ambuye wanga aonetsa

chisomo chake. Ndithudi Ambuye wanga amakhululukira
ndiponso ndi Wachisoni chosatha.”
54. Mfumu idati, “Mubweretseni iye kwa ine kuti
ndimusankhe iye kukhala munthu wanga.” Ndipo
atayankhula naye, Mfumu idati, “Ndithudi iwe udzakhala
ndi ife kuyambira lero ndipo udzakhala wolemekezeka
ndiponso wokhulupirika.” 55. Yosefe adati, “Ndiikeni pa
udindo woyang’anira nkhokwe za m’dziko. Ine, ndithudi,
ndidzazisunga bwino.” 56. Mmenemo ndi mmene
tidamupatsira Yosefe udindo mdziko ndipo adakhala
paliponse pamene amafuna. Ife timampatsa chisomo
amene tamufuna ndipo sitisokoneza mphotho za anthu
ochita zabwino. 57. Ndipo, ndithudi, mphotho ya m’moyo
umene uli nkudza ndi yabwino kwa anthu okhulupirira ndi
amene anali kuopa Mulungu.
58. Ndipo abale ake a Yosefe adadza, nalowa kwa iye.
Iye adawazindikira koma iwo sadamuzindikire iye.
59. Ndipo pamene iye adawakonzera chakudya chawo, iye
adati, “Ndibweretsereni m’bale wanu mwa abambo anu.
Kodi inu simukuona kuti ine ndikukwaniritsa muyeso
ndiponso ndimalandira bwino alendo?” 60. “Koma ngati
inu simudzabwera naye kwa ine inu simudzalandira
muyeso wa chakudya kuchokera kwa ine ndiponso
simudzandiyandikira.” 61. Iwo adati, “Ife tikawanyengerera
abambo ake kuti akamulole kuti adzabwere nafe. Ichi,
ndithudi, tikachita.”
62. Yosefe adawauza anyamata a ntchito ake kuti aike
ndalama zawo m’matumba mwawo kuti akazindikire
akakafika kwa abale awo kuti mwina akabwerenso.
63. Pamene iwo adabwerera kwa abambo awo iwo adati,

“Oh inu abambo athu! Kwaletsedwa kwa ife kugula
muyeso wachakudya. Motero mtumizeni m’bale wathu
pamodzi ndi ife kuti ife tikapeze muyeso wa chakudya.
Ndipo ife tikamusamala.” 64. Yakobo adati, “Kodi ine
ndikukhulupirireni pokupatsani uyu monga momwe
ndidakukhulupirirani kale ndi m’bale wake uja? Komatu
Mulungu ndiye Msungi wabwino ndipo Iye ndiye
wachifundo mwa achifundo onse.”
65. Ndipo pamene iwo adatsekula katundu wawo,
adapeza kuti ndalama zawo zabwezedwa kwa iwo.
Iwo adati, “Oh Atate athu! Kodi ndi chiyani chimene
tingafunenso? Nazi ndalama zathu zabwezedwa kwa ife
motero tidzapeza chakudya chambiri cha mabanja athu.
Ndiponso tidzamusamala m’bale wathu ndi kuonjezera
muyeso wokwana kunyamulidwa ndi ngamira imodzi.
Umenewu ndiwo muyeso wochepa.” 66. Iye adati, “Ine
sindidzamutumiza iye pamodzi ndi inu pokhapokha ngati
mutandipatsa lonjezo M’dzina la Mulungu, kuti mudzabwera
naye kwa ine kupatula ngati mutagonjetsedwa.” Ndipo
pamene iwo adapereka lonjezo lawo, iye adanena kuti, “Pa
zonse zimene tikunena, Mulungu akhale mboni.”
67. Ndipo iye adati, “E inu ana anga! Musakalowere
khomo limodzi koma kaloweni m’makomo osiyanasiyana
ndipo ine sindingakuthandizeni chilichonse polimbana
ndi Mulungu. Zoonadi chiweruzo ndi cha Mulungu yekha.
Mwa Iye yekha ine ndimaika chikhulupiriro changa
ndipo onse amene amakhulupirira aike chikhulupiriro
chawo mwa Iye.” 68. Pamene iwo adalowa, monga momwe
atate awo adawalangizira, sizidawathandize chilichonse
kwa Mulungu. Ichi sichinali china chilichonse koma

kungokwaniritsa chifuniro chimene Yakobo adali nacho.
Ndithudi iye adali ndi nzeru chifukwa Ife tidamuphunzitsa,
koma anthu ambiri sadziwa.
69. Ndipo pamene iwo adalowa kwa Yosefe, iye adamutenga
m'bale wake pambali nati, "Ndithudi ine ndine m'bale
wako ndipo usadandaule ndi zimene iwo adali kuchita."
70. Ndipo pamene iye adawakonzera chakudya chawo,iye
adaika mbale m'nthumba, la m'bale wake. Ndipo woitana
adafuula kwa iwo nati, "Oh inu apaulendo! Ndithudi inu
ndinu akuba!" 71. Iwo adatembenuka nati, "Kodi mwasowa
chiyani?" 72. Iwo adati, "Tikusowa mbale ya Mfumu ndipo
aliyense amene abweretse mbale adzalandira katundu
wokwana kunyamula ndi ngamira imodzi. Ndipo ine ndine
mboni." 73. Iwo adanena kuti, "Pali Mulungu! Ndithudi
inu muli kudziwa kuti ife sitinadze kudzaononga m'dziko
lanu ndipo sindife mbala ayi!" 74. Iwo adati, "Kodi chilango
chake ndi chotani, ngati inu mukunena zabodza?" 75. Iwo
adati: "Aliyense amene m'thumba mwake mupezeke mbale,
iyeyo ndiye adzalandira chilango cha mbaleyo. Kotero
ndimo mmene ife timalangira athu ochita zoipa." 76. Ndipo
iye adayamba kusanthula matumba awo asadasanthule
thumba la mng'ono wake. Ndipo pomaliza iye adaitulutsa
mbale ija m'thumba la mng'ono wakeyo. Mmenemo ndimo
tidamphunzitsira nzeru Yosefe chifukwa ndi ulamulo
wa m'dziko limenelo sakadatha kusunga m'bale wake
pokhapokha ngati Mulungu akadafuna kuti zichitike
motero. Ife timakweza paudindo amene tamufuna; koma
pamwamba pa iwo amene ali ndi nzeru, alipo ena amene
ndi odziwa kwambiri.
77. Iwo adati, "Ngati iye waba, ndiye kuti panali m'bale

wake wina amene adabanso kale." Koma Yosefe adasunga
chinsinsi ndipo sadawauze iwo ayi. Iye adaganiza kuti "Inu
muli pa mlandu. Mulungu ali kudziwa bwino zonse zimene
mukunena." 78. Iwo adati, "Oh inu Mfumu! Ndithudi iye
ali ndi abambo ake wokalamba kwambiri. Motero tengani
mmodzi wa ife m'malo mwake. Ndithudi ife tili kukuonani
kuti inu ndinu mmodzi wa anthu ochita zabwino."
79. Iye adati, "Mulungu ateteze kuti ife titenge wina wake
m'malo mwa munthu amene tam'peza ndi katundu wathu.
Ndithudi titatero tikhala opanda chilungamo."

80. Motero pamene iwo anada nkhawa ndi iye, iwo
adakhala paokha ndikunong'onezana. Ndipo wamkulu
wawo adati, "Kodi inu simudziwa kuti abambo anu
adatenga lonjezo kwa inu, M'dzina la Mulungu ndiponso
kuti mudaphwanya chikhulupiriro chanu kale ndi nkhani
ya Yosefe? Motero ine sindidzachoka m'dziko muno mpaka
pamene abambo anga andilola kapena kufikira pamene
Mulungu atapereka chiweruzo chake pa nkhani iyi. Iye
ndiye Muweruzi wabwino pa aweruzi onse." 81. "Bwererani
kwa atate wanu ndipo mukawauze kuti, "Oh Bambo wathu!
Ndithudi mwana wanu waba ndipo ife sitiikira umboni
kupatula pa zimene tikudziwa. Ndipo ife sitikadadziwa
zinthu zobisika!" 82. "Ndipo funsani anthu a mumzinda
umene tidali ndiponso apaulendo amene tafika nawo,
ndipo ndithudi ife tili kunena zoonadi."

83. Yakobo adati, "Iyayi! Mizimu yanu yakunyengani
kuchita zoipa. Koma kupirira ndi kwabwino. Mwina
Mulungu adzawabweretsa onse awiri kwa ine. Ndithudi
Iye yekha amadziwa zinthu zonse ndiponso ndi waluntha."
84. Ndipo iye adayang'ana kumbali nati, "Kalanga! Ine

ndili ndi chisoni ndi Yosefe!" Maso ake adachita khungu chifukwa cha chisoni chachikulu chimene chinali mu mtima mwake. 85. Ana ake adati, "Pali Mulungu! Inu simudzasiya kumukumbukira Yosefe mpaka mufoka ndi ukalamba kapena mufa." 86. Iye adati, "Ine ndili kudandaula kwa Mulungu za chisoni changa ndipo ndilikudziwa kuchokera kwa Mulungu zimene inu simukuzidziwa." 87. "Oh ana anga!, Pitani mukafufuze za Yosefe pamodzi ndi m'bale wake, ndipo musataye mtima ndi chisomo cha Mulungu. Ndithudi palibe amene amataya mtima ndi chisomo cha Mulungu kupatula anthu osakhulupirira."

88. Ndipo pamene iwo adalowa kwa Yosefe, iwo adati, "Oh inu Mfumu yolemekezeka! Ife pamodzi ndi anthu athu tapeza mavuto, ndipo ife tabweretsa ndalama zochepa motero tiyesereni chakudya chokwanira ndipo tipatseni china chaulere. Ndithudi Mulungu amalipira anthu ochita zabwino." 89. Iye adati, "Kodi inu muli kudziwa zimene mudamuchitira Yosefe ndi m'bale wake pamene inu simumadziwa?" 90. Iwo adati, "Kodi iwe ndiwedi Yosefe?" Iye adati, "Ine ndine Yosefe ndipo uyu ndi m'bale wanga. Mulungu, ndithudi, watikomera mtima ife. Ndithudi iye amene amaopa Mulungu ndi kupirira molimba ndithudi Mulungu sasokoneza malipiro a anthu ochita zabwino."

91. Iwo adati, "Pali Mulungu, ndithudi, Mulungu wakulemekezani inu kuposa ife ndipo, ndithudi, ife tidali olakwa." 92. Iye adati, "Palibe chidzudzulo kwa inu tsiku lalero ndipo Mulungu akukhululukireni inu. Iye ndiye wokhululukira mwa okhululukira onse." 93. "Pitani ndi malaya angawa ndipo mukawaponye pamaso pa abambo

anga ndipo maso awo adzayambanso kuona. Ndipo
mukabwere, ndi abale anu onse kwa ine."
94. Ndipo pamene gulu la a paulendo lidanyamuka, atate
awo adati, "Ndikumva fungo la Yosefe ngati inu muganiza
kuti nzeru zanga zatha." 95. Iwo adati, "Pali Mulungu! Iwe
ndiwe wosokonekera kuyambira kale." 96. Ndipo pamene
mthenga wa nkhani zabwino adadza iye adaponya malaya a
Yosefe pamaso pake, ndipo nthawi yomweyo adayambanso
kupenya. Iye adati, "Kodi ine sindidakuuzeni kuti ine
ndinali kudziwa, kuchokera kwa Mulungu, zinthu zimene
inu simuzidziwa?" 97. Iwo adati, "Oh abambo athu!
Tipemphereni chikhululukiro cha machimo athu, ndithudi,
ife tidali ochimwa." 98. Iye adati, "Ine ndidzakupempherani
chikhululukiro kwa Ambuye wanga. Ndithudi Iye ndi
wokhululukira ndiponso ndi Wachisoni chosatha."
99. Ndipo pamene iwo adalowa kwa Yosefe iye adatenga
makolo ake pa yekha nati, "Lowani mu dziko la Aiguputo,
ngati Mulungu afuna, mwamtendere." 100. Ndipo iye
adanyamula makolo ake ndikuwakhazika pa mpando
wolemekezeka ndipo onse adagwa pansi kulemekeza iye.
Ndipo iye adati, "Oh bambo wanga! Ili ndi tanthauzo
la maloto anga aja akale. Ndithudi Ambuye wanga
adawapanga kukhala oona. Iye adandichitira ine ubwino
pamene adanditulutsa kundende ndipo adakubweretsani
inu kuchokera ku midzi pambuyo pakuti satana
adakhazikitsa udani pakati pa ine ndi abale anga. Ndithudi
Ambuye wanga ndi waulemu ndi wachisoni kwa amene Iye
wamufuna. Ndithudi! Iye yekha ndi wodziwa zonse ndi
wanzeru."
101. "Ambuye, Inu ndithudi, mwandipatsa ine ulemerero

ndi kundiphunzitsa kutanthauzira maloto. Inu ndinu Namalenga wakumwamba ndi dziko lapansi. Inu ndinu Msungi wanga m'dziko lino ndiponso m'dziko limene lili nkudza. Ndilekeni kuti ndife ndili kukulambirani inu ndipo ndiikeni m'gulu la anthu abwino."

102. Chimene tavumbulutsa kwa iwe ndi mbiri yakale yachinsinsi. Iwe kudalibe pamene abale ake a Yosefe onse adakonza chiwembu. 103. Ndipo anthu ambiri sadzakhulupirira ngakhale ungalimbikire motani. 104. Iwe siuwafunsa malipiro chifukwa cha ichi. Ichi ndi chizindikiro ndi chikumbutso kwa anthu a mitundu yonse.

105. Kodi ndi zizindikiro zingati za mu mlengalenga ndi za m'dziko lapansi zimene iwo amangozipyola osalabadira china chilichonse? 106. Ndipo ambiri a iwo sakhulupirira mwa Mulungu kupatula kupembedza milungu ina yoonjezera pa Mulungu weniweni. 107. Kodi iwo amaganiza kuti ndi otetezedwa ku chilango cha Mulungu kuti chilango chake sichidzadza pa iwo mwadzidzidzi opanda kuzindikira? 108. Nena, "Iyi ndi njira yanga. Ine mosakayika, ndili kukuitananí ndi nzeru kuti mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, ine pamodzi ndi onditsatira anga. Ulemerero ukhale kwa Mulungu ndipo ine sindine wopembedza mafano ayi."

109. Ndipo Ife sitinatumizepo iwe usanadze, wina kupatula anthu amene tinawatsogolera kuchokera pakati pa anthu a m'mizinda. Kodi iwo sanayende padziko ndi kuona zimene zidawachitikira amene adalipo kale? Ndipo, ndithudi, moyo umene uli nkudza ndi wabwino kwa anthu amene amaopa Mulungu ndipo amamumvera Iye. Kodi mulibe nzeru? 110. Mpaka pamene Atumwi athu adataya

mtima ndipo anali kuganiza kuti kulibe wina aliyense amene akadawakhulupirira iwo, thandizo lathu lidadza pa iwo ndi kupulumutsa aliyense amene Ife tidamufuna. Ndipo chilango chathu sichingabweretsedwe m’mbuyo kwa anthu ochita zoipa.

111. Ndithudi m’mbiri yawo muli phunziro kwa anthu ozindikira. Iyi si nkhani yopeka ayi koma ndi chitsimikiziro cha ma buku a Mulungu amene adaperekedwa kale, ndipo ndi mfotokozi wa zinthu zonse ndi chilangizo ndiponso madalitso kwa anthu okhulupirira.

Sura 13 • Ar-Ra‘d

# Al-Ra’d

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. *Alif Lam Mim Raa.*

Awa ndi mavesi a Buku. Chimene chavumbulutsidwa
kwa iwe kuchokera kwa Ambuye wako ndi choonadi.
Koma anthu ambiri sakhulupirira. 2. Mulungu ndi amene
adakweza mlengalenga popanda nsanamira yomwe
mungaione. Ndipo Iye adabuka pamwamba pa Mpando
wa Chifumu ndipo adalamulira dzuwa ndi mwezi, ndipo
chilichonse chimayenda monga momwe chidalamulidwira
kufikira munthawi yake. Iye amalamulira zinthu zonse
ndipo amafotokoza chivumbulutso chake momveka kuti
inu mukhulupirire zoti mudzakumana ndi Ambuye wanu.
3. Iye ndiye amene adatambasula dziko lapansi ndi kuika

mu ilo mapiri ndi mitsinje. Ndipo pa mtundu uliwonse wa
zipatso, adazilenga ziwiriziwiri. Iye amapanga usiku kuti
uzivundikira usana. Ndithudi mu izi muli zizindikiro kwa
anthu oganiza.
4. Ndipo m'dziko muli njira zoyandikirana ndi minda ya
mitengo ya mphesa ndi minda yobzalidwa ndi chimanga,
nkhalango za mitengo ya tende, zofanana ndi zina
zosafanana. Zipatso zake zimathiriridwa ndi madzi a
mtundu umodzi: Ife timazipanga zina kukhala zabwino
kupitirira zinzake pakudya. Ndithudi mu zimenezi muli
zizindikiro kwa anthu oganiza.
5. Ngati iwe ukudabwa, zodabwitsa kwambiri ndi mawu
awo oti, "Ife tikadzakhala dothi, kodi tidzalengedwanso
kwatsopano?" Amenewa ndiwo sadakhulupirire Ambuye
wawo. Iwo ndiwo amene adzakhala ndi unyolo wa zitsulo
umene udzamangiririridwa manja ku makosi awo. Amenewo
ndi anthu akumoto ndipo iwo adzakhalako mpaka kalekale.
6. Iwo ali kukuchititsa iwe kuti uchite choipa m'malo
mwa chinthu chabwino. Komatu ndi anthu ambiri amene
adalangidwa iwo asanadze. Ndithudi Ambuye wako
amaonetsa chifundo kwa anthu ngakhale kuti iwo ndi
ochimwa. Ndithudi Ambuye wako amalangiratu.
7. Anthu osakhulupirira amanena kuti, "Bwanji
sichinatumizidwe chizindikiro chochokera kwa Ambuye
wake?" Iwe ndiwe mchenjezi basi ndipo mtundu uliwonse
uli ndi mlangizi wawo.
8. Mulungu amadziwa chinthu chilichonse chimene chili
m'mimba mwa chachikazi ndi chimene chili choperewera
ndiponso chimene chimabadwa nthawi yake isanakwane
kapena itapitirira. Ndipo chithu chilichonse kwa Iye, chili

ndi muyeso wake. 9. Iye amadziwa zinthu zonse zooneka
ndi zosaoneka. Iye ndi Wamkulu ndi wapamwamba
kwambiri. 10. Ndi chimodzimodzi kaya wina wa inu
ayankhula monong’ona kapena mokweza kaya adzibisa mu
mdima kapena ayenda usana.
11. Aliyense ali ndi angelo amene amakhala patsogolo
ndi pambuyo pake. Iwo amamuyang’anira iye potsatira
malamulo a Mulungu. Ndithudi! Mulungu sadzasintha
chikhalidwe cha anthu pokhapokha iwo eni ake asintha
makhalidwe awo. Koma ngati Mulungu afuna kulanga
anthu, palibe amene angathawe ndipo iwo sadzapeza wina
kupatula Iye amene angawateteze!
12. Iye ndiye amene amakuonetsani mphenzi ngati
choopsa ndi chobweretsa chiyembekezo. Ndipo
Iye amasonkhanitsa mitambo yolemera. 13. Mabingu
amamuyamika Iye ndipo angelo nawo amamuyamika ndipo
amamuopa Iye kwambiri. Iye amaponya ziphaliwali ndipo
ndi ziphaliwalizo amaononga aliyense amene wamufuna
ngakhale kuti anthu osakhulupirira amatsutsa za Mulungu.
Iye ndi wamphamvu zonse ndipo amalanga kwambiri.
14. Kwa Iye kuli mawu a choonadi. Ndipo zimene iwo
amazipembedza siziwayankha china chilichonse monga
momwe munthu amene amatambasula manja ake ku madzi
ndi kumawaitana kuti alowe m’kamwa mwake. Koma
madzi sangathe kulowa m’kamwa! Ndipo mapemphero a
anthu osakhulupirira ndi opanda phindu.
15. Onse amene amakhala kumwamba ndi pa dziko
lapansi amagwa pansi kugwadira Mulungu, mwachifuniro
chawo kapena mokakamizidwa. Ndipo zithunzi zawo
zimamugwadira Iye m’mawa ndi madzulo aliwonse.

16. Nena, "Kodi Ambuye wakumwamba ndi pa dziko lapansi ndani?" Nena, "Mulungu." Nena, "Kodi inu mwasankha milungu ina yoonjezera pa Mulungu weniweni imene, ngakhale kwa iyo yokha, singathe kuchita zinthu zoipa kapena zabwino?" Nena, "Kodi anthu a khungu ndi anthu oona ndi ofanana? Kapena mdima umafanana ndi kuwala? Kodi iwo akuphatikiza Mulungu ndi mafano awo? Kodi mafano awo adalenga zinthu zofanana ndi zimene Iye adalenga; kotero kuti zolengedwa zonse zimaoneka kwa iwo ngati zofanana?" Nena, "Mulungu ndi Namalenga wa zinthu zonse. Iye ndi Mmodzi yekha ndipo ndi Mwini Mphamvu zonse."

17. Iye amagwetsa mvula kuchokera kumwamba ndipo madzi amayenda m'madambo molingana ndi muyeso wake. Ndipo madzi oyenda amapanga thovu lokwera. Ndipo kuchokera ku zitsulo zimene anthu amatenthetsa pa moto pofuna zinthu zodzikongoletsera ndi zodzisangalatsira, mumatuluka thovu chimodzimodzi. Mmenemo ndi mmene Mulungu amaonetsera poyera choona ndi chabodza. Likakhala thovu limatayidwa, pamene chimene chili chabwino kwa anthu chimatsala pa dziko. Kotero ndi mmene Mulungu amaperekera zitsanzo.

18. Iwo amene adayankha kuitana kwa Ambuye wawo ali ndi mphotho yamtengo wapatali. Koma iwo amene adakana kuitana kwake, ngakhale kuti akadakhala ndi chuma chonse chimene chili pa dziko lapansi ndi china choonjezera kuti chikakhale ngati dipo lawo; chawo chidzakhala chiweruzo choipa. Gahena ndiyo idzakhala mudzi wawo womwe ndi malo onyansa okhalamo.

19. Kodi iye amene adziwa chimene chavumbulutsidwa

kwa iwe kuchokera kwa Ambuye wako kuti ndi choonadi ndi
olingana ndi iye amene ali wakhungu? Ndi okhawo amene
ali ndi nzeru amene azindikira. [20] Iwo amene amakwaniritsa
lonjezo la Mulungu ndipo saphwanya lonjezolo. [21] Iwo
amene amalumikiza chimene Iye wawalamula kuti
chikhale chimodzi, amaopa Ambuye wawo ndipo amaopa
zoopsa zimene zidzaoneka patsiku lachiweruzo. [22] Ndi
iwo amene amapirira chifukwa chofuna mtendere wa
Mulungu modzipereka, amapitiriza mapemphero awo ndi
kupereka zimene tawapatsa mseri kapena moonekera,
ndipo amaletsa choipa pochita chinthu chabwino. Awa
ndiwo amene adzaone zinthu zokoma. [23] Iwo adzalowa
ku Paradiso kwa muyaya pamodzi ndi ena a makolo awo
angwiro, ndi akazi awo ndi ana awo. Kuchokera ku khomo
lililonse angelo adzadza nati kwa iwo. [24] “Mtendere ukhale
pa inu chifukwa cha kupirira kwanu pa mavuto ochuluka.
Yodalitsika ndi mphotho ya ku Paradiso!”

[25] Iwo amene amaphwanya lonjezo la Mulungu atalilandira
ndipo amalekanitsa zinthu zimene Iye adawalamulira
kuti azilumikize, ndipo amachita zinthu zoipa pa dziko
lapansi, temberero lidzaikidwa pa iwo ndipo malo awo
okhala adzakhala osasangalatsa. [26] Mulungu amapereka
mowolowa manja kwa aliyense amene Iye wamufuna ndi
monyalapsa ndipo iwo amasangalala m’moyo uno pamene
chisangalalo cha m’moyo uno ndi cha kanthawi kochepa
kwambiri pofanizira ndi cha moyo umene uli nkudza.

[27] Ndipo iwo amene sakhulupirira amati, “Kodi
ndi chifukwa chiyani chizindikiro sichidaperekedwe
kuchokera kwa Ambuye wake?” Nena, “Ndithudi
Mulungu amasocheretsa aliyense amene wamufuna

ndipo amatsogolera onse amene amalapa kwa Iye."
28. Iwo ndi amene amakhulupirira ndipo mitima yawo imapeza mpumulo akamakumbukira Mulungu. Ndithudi m'chikumbukiro cha Mulungu mitima imapeza mpumulo.
29. Iwo amene amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino adzasangalala ndipo mapeto awo adzakhala okoma.

30. Kotero Ife takutumiza iwe ku mtundu wa anthu umene anthu ake ena adafa kale kuti ulakatule kwa iwo chivumbulutso chathu chimene tidavumbulutsa kwa iwe. Pamene iwo sakhulupirira mwa mwini chifundo. Nena "Iye ndiye Ambuye wanga. Kulibe Mulungu wina kupatula Iye yekha. Mwa Iye ine ndimadalira ndipo ndi kwa Iye kumene ine ndidzabwerera."

31. Ndipo ngati pakadakhala Korani imene ikadayendetsa mapiri, kapena ikadaphwanya nthaka kapena kuwapanga anthu akufa kuti ayankhule ikanakhala Korani inoyi. Zinthu zonse zimayendera chifuniro cha Mulungu. Kodi anthu okhulupirira sadziwa kuti Mulungu, akadafuna akadatsogolera anthu a mitundu yonse? Ndipo tsoka silidzaleka kugwa pa iwo amene sakhulupirira chifukwa cha ntchito zawo zoipa kapena ilo lidzakhala pafupi ndi midzi yawo mpaka pamene lonjezo la Mulungu likwaniritsidwa.
32. Ndipo ndithudi Atumwi ambiri adanyozedwa iwe usanadze ndipo Ine ndidawalekerera anthu osakhulupirira, ndipo pomaliza ndidawalanga. Kodi chilango changa chidali chowawa bwanji?

33. Kodi Iye amene amayang'anira mizimu yonse ndi ntchito zonse zimene imachita angafanane ndi wina wosadziwa? Komabe iwo amakhazikitsa milungu ina

m'malo mwa Mulungu weniweni. Nena, "Itchuleni! Kodi
inu mungamuuze Mulungu zinthu zimene Iye sadziwa pa
dziko kapena iwo ndi mawu abodza chabe?" Iyayi. Kwa
iwo amene sakhulupirira, chiwembu chawo chimaoneka
chabwino ndipo iwo atsekerezedwa kutsatira njira yoyenera
ndipo aliyense amene Mulungu amamusocheza, kwa iye
kulibe amene angamutsogolere. 34. Iwo ali ndi chilango
mmoyo uno, ndipo, ndithudi, chilango chowawa kwambiri
ndi chimene chili m'moyo umene uli nkudza. Ndipo iwo
alibe amene adzawateteza kwa Mulungu.
35. Chitsanzo cha Paradiso imene anthu oopa Mulungu
adalonjezedwa, pansi pake pamadutsa mitsinje; zipatso
zake ndi zosatha ndi mithunzi yake ndi yosathanso.
Imeneyi ndiyo mphotho ya anthu oopa Mulungu. Koma
mphotho ya anthu osakhulupirira ndi moto.
36. Iwo amene tidawapatsa Buku, amasangalala ndi
zimene zavumbulutsidwa kwa iwe koma pali kagulu
kena kamene kamakana zina mwa izo. Nena, "Ine
ndalamulidwa kupembedza Mulungu mmodzi ndipo kuti
ndisamuphatikize Iye ndi chinthu china chilichonse.
Ndi kwa Iye kumene ndimapempha ndipo kwa Iye
ndidzabwerera." 37. Kotero Ife talitumiza pansi kukhala
chiweruzo champhamvu m'chiyankhulo cha Chiarabu.
Ngati iwe utsatira zofuna zawo pamene utapatsidwa
nzeru, palibe amene adzakupulumutsa kapena kukuteteza
kwa Mulungu. 38. Ndithudi Ife tidatumiza Atumwi iwe
usanadze ndipo tidawapatsa akazi ndi ana. Koma padalibe
Mtumwi amene amabweretsa zizindikiro zozizwitsa
popanda chilolezo cha Mulungu. Chilichonse chili ndi
nthawi yake. 39. Mulungu amafafaniza chimene Iye afuna

kapena amakhazikitsa. Ndipo kwa Iye ndi kumene kuli
Manthu wa Buku.
40. Kaya tikuonetsa zina mwa zimene tikuwalonjeza
kapena tikupha chilangocho chisanadze, udindo wako ndi
kufalitsa uthenga, ndipo kwa Ife ndiko kuli chiwerengero.
41. Kodi iwo saona mmene Ife timachepetsera malire a dziko
pang'onopang'ono? Ndipo Mulungu akalamulira chinthu,
palibe amene angatsutse. Iye ndi wachangu powerengera.
42. Ndithudi iwo amene adalipo awa asanadze nawonso
adali kuchita ziwembu koma chikonzero chonse ndi cha
Mulungu. Iye amadziwa chimene aliyense amalandira
ndipo anthu osakhulupirira adzadziwa kuti kodi ndani
amene adzalandira ubwino pomaliza.
43. Ndipo iwo amene sakhulupirira amati, "Iwe sindiwe
Mtumwi." Nena, "Mulungu akukwanira kukhala mboni
pakati pa ine ndi inu ndi iwo amene amadziwa za m'Buku."

Sura 14 • Ibrâhîm

# Ibrahim

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. *Alif Lam Ra.*

Tavumbulutsa Buku lino kwa iwe kuti uwatulutse anthu
kuchoka kumdima ndi kupita kowala, kunjira ya Mwini
Mphamvu, ndi Mwini kuyamikidwa mwachifuniro cha
Ambuye wawo. 2. Mulungu ndiye Mwini wa zonse zimene
zili kumwamba ndi dziko lapansi. Tsoka kwa anthu

osakhulupirira chifukwa cha chilango chowawa. 3. Iwo
amene amakonda moyo uno kuposa moyo umene uli nkudza
ndipo amaletsa kutsatira njira ya Mulungu ndipo amafuna
za chinyengo mu izo, iwo ndi wosochera kwambiri.

4. Ndipo Ife sitinatumize Mtumwi kupatula m'chilankhulo
cha anthu ake ndi cholinga chakuti akhoza kuwafotokozera
momveka. Ndipo Mulungu amasocheretsa aliyense amene
Iye wamufuna ndi kutsogolera amene wamufuna. Ndipo
Iye ndiye Mwini mphamvu zonse ndiponso Mwini luntha.

5. Ndithudi Ife tidamutuma Mose ndi zizindikiro zathu
ndi kunena kuti, "Atulutse anthu ako kuchoka ku mdima
ndi kupita nawo kowala ndipo uwakumbutse za masiku a
Mulungu." Ndithudi mu izi muli zizindikiro kwa aliyense
wopirira ndi wothokoza.

6. Ndipo pamene Mose adawauza anthu ake kuti,
"Kumbukirani ubwino wa Mulungu kwa inu pamene
Iye adakupulumutsani inu kwa anthu a Farawo, amene
adakupatsani inu mavuto aakulu ndipo anali kupha ana
anu aamuna ndi kusiya ana anu aakazi amoyo, ndithudi,
zimenezi zidali mayesero aakulu kuchokera kwa Ambuye
wanu." 7. Ndipo pamenepo Ambuye wanu adalengeza
kuti, "Ngati inu muthokoza, Ine ndidzakupatsani zinthu
zambiri koma ngati simuthokoza, ndithudi, chilango
changa ndi chokhwima kwambiri." 8. Ndipo Mose adati
"Ngati inu simukhulupirira, inu ndi wonse amene ali
padziko lapansi, ndithudi, Mulungu ndi wolemera ndipo
ndi Mwini kuyamikidwa."

9. Kodi inu simunamve nkhani za anthu a Nowa, Aad,
ndi Thamoud omwe adalipo inu musanadze? Ndiponso za
iwo amene adadza pambuyo pawo? Palibe adziwa za iwo

kupatula Mulungu yekha. Atumwi awo adadza kwa iwo ndi
zizindikiro zooneka koma iwo adatseka pakamwa pawo
ndi manja awo ndipo adati, "Ndithudi ife sitikhulupirira
mu zimene mwatumidwa, ndithudi ife tili ndi chikaiko
pazimene mukutiitanira."
10. Atumwi awo adati, "Chiyani! Kodi pangakhale
chikayiko pa Mulungu, Namalenga wa kumwamba ndi
dziko lapansi? Iye akukuitanani kuti akukhululukireni
machimo anu ndi kukusungani mpaka pa nthawi yomwe
idaikidwa." Iwo adati, "Inu simuli ena, koma anthu ngati
ife. Inu mufuna kutiletsa zimene makolo athu anali
kupembedza. Tipatseni umboni weniweni wooneka."
11. Atumwi awo adati kwa iwo, "Ife tili anthu ngati inu
nomwe koma Mulungu amakhazikitsa chisomo chake
pa ena mwa akapolo ake amene Iye wawasankha. Ife
sitingathe kukupatsani chizindikiro pokhapokha ngati
Mulungu afuna. Mwa Mulungu yekha onse okhulupirira
aike chikhulupiriro chawo." 12. "Kodi ife tingalekerenji
kuika chikhulupiriro chathu mwa Mulungu pamene Iye
watitsogolera kunjira zathu? Ndithudi ife tidzapirira ku
mazunzo amene mungatipatse ife ndipo mwa Mulungu,
onse amene amakhulupirira aike chikhulupiriro chawo."
13. Ndipo anthu osakhulupirira adati kwa Atumwi awo,
"Ndithudi ife tidzakuthamangitsani m'dziko lathu kapena
mubwerere kuchipembedzo chathu." Koma Ambuye
wawo adawalangiza iwo nati, "Ndithudi tidzaononga anthu
ochita zoipa." 14. "Ndipo, ndithudi, tidzakukhazikitsani
m'dziko pambuyo pa iwo. Chimenechi ndi cha iye amene
aopa kudzaima pamaso panga ndipo amaopa chenjezo
langa."

15. Ndipo iwo adafunafuna kupambana ndi chithandizo
ndipo aliyense wamwano, wamtudzu ndi wolamula
mwankhanza, adatayika ndi kuonongeka. 16. Kutsogolo
kwake kuli Gahena ndipo adzamwetsedwa madzi owira
ndi othukusira. 17. Iye, mwa unyizi, adzangopsontha koma
sadzamwa ngakhale ndi pang'ono pomwe, ndipo imfa
idzadza kuchokera kumbali zonse koma iye sadzafa ayi
ndipo chilango chowawa chidzakhala kutsogolo kwake.

18. Fanizo la iwo amene sakhulupirira mwa Ambuye wawo
ndi lakuti ntchito zawo zili ngati phulusa limene liulutsidwa
ndi mphepo pa tsiku la mphepo ya mkuntho. Iwo sadzapeza
china chilichonse kuchokera ku zinthu zimene ankachita.
Ndipo kumeneku ndiko kusochera kwenikweni. 19. Kodi
iwe siuona kuti Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko
lapansi mwachoonadi? Atafuna Iye akhoza kukuchotsani
ndi kubweretsa zolengedwa zatsopano. 20. Kwa Mulungu
zoterezo si zovuta ayi.

21. Ndipo onse adzaonekera pa maso pa Mulungu. Ndipo
anthu ochepa mphamvu adzanena kwa iwo amene anali a
mwano kuti, "Ndithudi ife tinali kutsatira inu. Kodi inu
mungatiteteze ife ku chilango cha Mulungu?" Iwo adzati,
"Mulungu akadatitsogolera ife tikadakutsogolerani inu.
Ndi chimodzimodzi kwa ife kaya tikalipa kapena tipirira,
tilibe kothawira."

22. Ndipo Satana adzanena, pamene chiweruzo
chaperekedwa, kuti: "Ndithudi Mulungu adakulonjezani
lonjezo loona. Inenso ndidakulonjezani koma
ndidakusocheretsani. Ine ndidalibe udindo pa
inu, kupatula kuti ndidangokuitanani ndipo inu
mudandiyankha. Tsopano musandidzudzule ine ayi koma

dzidzudzuleni nokha. Ine sindingathe kukuthandizani
ndipo inu simungandithandize ine. Ndithudi ine ndakana
kundisakaniza kwanu ndi Mulungu kumene munali
kuchita." Zoonadi ochita zoipa adzalangidwa zedi.
23. Ndipo iwo amene adakhulupirira ndipo amachita
ntchito zabwino, adzalowetsedwa ku minda yothiriridwa
ndi madzi yam'mitsinje ndipo adzakhala komweko mpaka
kalekale ndi chilolezo cha Ambuye wawo. Kulonjerana
kwawo kudzakhala "Mtendere".
24. Kodi simuona mmene Mulungu amaperekera
chitsanzo? Liwu labwino lili ngati mtengo wabwino
umene mizu yake ndi yokhazikika ndi nthambi zake zifika
mlengalenga. 25. Umene umabereka zipatso nyengo iliyonse
ndi chilolezo cha Ambuye wake ndipo Mulungu amapereka
mafanizo kwa anthu ndi cholinga chakuti azikumbukira.
26. Ndipo chitsanzo cha liwu loipa lili ngati mtengo woipa,
umene uzulidwa kuchoka ku nthaka ndipo ulibe mizu ina
iliyonse.
27. Mulungu adzalimbikitsa anthu okhulupirira ndi liwu
lokhazikika m'moyo uno ndi m'moyo umene uli nkudza.
Ndipo Mulungu adzasocheretsa ochita zoipa ndipo
Mulungu amachita zimene Iye afuna.
28. Kodi siunaone iwo amene amasinthanitsa chisomo
cha Mulungu ndi kusakhulupirira ndi kuwakankhizira
anthu awo kuti akhale m'nyumba ya mazunzo? 29. Ndipo
Gahena, m'mene iwo akalowe, ndi malo oipa kukhalako.
30. Iwo akhazikitsa milungu yabodza kuti ikhale yofanana
ndi Mulungu ndi cholinga chosokoneza anthu ku njira
yake. Nena, "Basangalalani! Koma, ndithudi, kokafikira
kwanu ndi ku Moto."

31. Auze akapolo anga, amene ali okhulupirira kuti
apitirize mapemphero ndi kupereka zothandiza osauka
kuchokera ku zimene tawapatsa mseri ndi pooneka,
lisanafike tsiku limene sikudzakhala kukambirana kapena
kuchita ubwenzi.
32. Ndi Mulungu amene adalenga kumwamba ndi dziko
lapansi ndipo amagwetsa madzi kuchokera kumwamba
amene amameretsa zipatso kuti zikhale chakudya chanu.
Iye adapanga zombo kuti muzizigwiritsa ntchito; kuti
zikhoza kuyenda pa nyanja ndi chilolezo chake ndipo
adapanga mitsinje kuti izikutumikirani. 33. Ndipo adalenga
dzuwa ndi mwezi, zimene zimayenda mokhazikika
m'misewu yawo kuti muzigwiritsa ntchito. Ndipo adalenga
usiku ndi usana kuti muziugwiritsa ntchito. 34. Ndipo Iye
adakupatsani zonse zimene mudamupempha ndipo ngati
inu muwerenga zokoma za Mulungu inu simungathe
kuziwerenga zonse. Zoonadi munthu ndi wosayamika ndi
wosakhulupirira.
35. Ndipo pamenepo Abrahamu adati, "Oh Ambuye
wanga! Upangeni uwu kukhala Mzinda wamtendere ndipo
nditetezeni ine ndi ana anga kuti tisapembedze mafano."
36. "Oh Ambuye wanga! Ndithudi mafano asocheretsa
anthu ambiri. Koma iye amene anditsatira ine ndithudi
adzakhala wa ine. Koma aliyense amene sandimvera ine,
komabe Inu ndinu okhululukira ndi wachisoni chosatha."
37. "Oh Ambuye wathu! Ine ndakhazika ena mwa ana anga
m'dambo lopanda zomera limene lili pafupi ndi Nyumba
yanu yoyera, Oh Ambuye wathu, kuti iwo azipemphera.
Motero dzazani mitima ya anthu ndi chikondi kuti

awaonetsere iwo ndipo apatseni iwo zipatso kuti akhale
othokoza."
38. "Oh Ambuye wathu! Ndithudi inu mumadziwa zonse
zimene timazibisa ndi zonse zimene timaulula. Palibe china
pa dziko lapansi kapena kumwamba chimene chimabisika
kwa Mulungu." 39. "Kuyamikidwa konse ndi kwa Mulungu
amene wandipatsa ine Ishimayeli ndi Isake ku ukalamba
wanga. Ndithudi! Ambuye wanga ndiye amene amamva
mapemphero onse." 40. "Oh Ambuye wanga! Ndipangeni
ine kukhala mmodzi wopemphera ndiponso kuchokera
ku ana anga. Ambuye wathu! Landirani pempho langa."
41. "Ambuye wathu! Khululukireni ine ndi makolo
anga ndi onse okhulupirira pa tsiku limene zonse
zidzakhazikitsidwa."
42. Usaganize kuti Mulungu sadziwa ntchito za anthu
ochita zoipa koma Iye akungowasiya mpaka patsiku
limene maso awo adzaona motuzuka. 43. Iwo adzathamanga
kupita kutsogolo, makosi osololoka, mitu yokwezedwa ndi
maso awo otuzuka ndipo mitima yawo idzakhala yopanda
chilichonse.
44. Achenjeze anthu za tsiku limene chilango chidzadza
pa iwo ndipo anthu ochita zoipa adzati, "Ambuye wathu
tipatseni mpumulo wa kanthawi kochepa ndipo ife
tidzamvera kuitana kwanu ndi kutsatira Atumwi anu."
Koma adzati kwa iwo, "Kodi inu nthawi zina simudalumbira
kuti simudzafa?" 45. Inu mumakhala m'nyumba za anthu
amene adachimwira miyoyo yawo pamene mumadziwa
zonse zimene tidawachitira iwo. Ndipo Ife tidakuikirani
chitsanzo. 46. Ndithudi iwo akonza chiwembu chawo

ndipo chiwembu chawo chili ndi Mulungu ngakhale kuti
chiwembu chawo chinali choti, chingathe kuchotsa mapiri.
47. Musaganize kuti Mulungu adzalephera kukwaniritsa
lonjezo lake limene adapereka kwa Atumwi ake. Ndithudi
Mulungu ali ndi mphamvu ndipo amatha kulanga. 48. Pa
tsiku limene dziko lapansi lidzasinthidwa kukhala dziko
lapansi la mtundu wina, ndi kumwamba kukhala kwa
tsopano, mtundu onse udzaonekera pamaso pa Mulungu,
Mmodzi yekha yemwe ndi Mwini mphamvu zonse.
49. Pa tsiku limeneli iwe udzaona anthu osakhulupirira
atamangidwa m'magoli. 50. Zovala zawo zidzakhala zakuda
ngati phula ndi nkhope zawo zidzakutidwa ndi malawi a
moto. 51. Kuti Mulungu alipire munthu aliyense pa zimene
adachita. Ndithudi Mulungu ndi wachangu powerengera.
52. Uwu ndi uthenga kwa anthu onse kuti achenjezedwe
nawo ndi kudziwa kuti Mulungu ndi mmodzi yekha ndi
kuti anthu anzeru akumbukire.

Sura 15 • Al-Hijr

# AL-HIJR

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. *Alif Lam Ra.*

Awa ndi mavesi a Buku, ndipo ndi Korani yofotokoza
bwino. 2. Mwina iwo amene sakhulupirira adzafuna kuti
akadakhala Asilamu. 3. Alekeni kuti adye, ndi kuti asangalale
ndipo alekeni kuti atangwanike ndi chikhulupiriro

chabodza. Iwo adzadziwa posachedwapa. 4. Ndipo Ife
sitinaonongepo mzinda wina uliwonse, kupatula pamene
nthawi yake itakwana. 5. Anthu sangathe kufulumizitsa
chiononongeko chawo kapena kuchichedwetsa ayi.

6. Iwo amati, “Iwe, amene Korani yavumbulutsidwa
kwa iwe! Ndithudi ndiwe munthu wa misala.” 7. “Bwanji
siutibweretsera angelo ngati iweyo uli mmodzi mwa
onena zoona?” 8. Ife sitimatsitsa pansi angelo, kupatula ndi
choonadi ndipo zitatero iwo sadzapatsidwa nthawi.

9. Ndithudi ndife amene tidatsitsa Korani ndipo,
ndithudi, Ife ndife amene tidzaiteteza.

10. Ndithudi Ife tidatumizapo, iwe usanadze, Atumwi ena
pakati pa mibadwo yakale. 11. Ndipo sikunadze kwa iwo
Mtumwi, amene iwo sanamuchite chipongwe. 12. Kotero
timalowetsa chisokonezo m’mitima ya anthu ochita zoipa.
13. Iwo sangakhulupirire mu uthenga wa Korani ndipo ndi
chizolowezi cha anthu amene adalipo kale. 14. Ndipo ngati
Ife tikadatsekula khomo lakumwamba, iwo ndi kumakwera
kumwamba mosalekeza. 15. Iwo akadakanabe kuti, “Maso
athu athobwa. Ndithudi ife talodzedwa.”

16. Ndithudi Ife taika nyenyezi zikuluzikulu kumwamba
ndipo tazikongoletsa kuti zizikondweretsa anthu
oyang’ana. 17. Ndipo tawateteza malo a kumwamba
kwa Satana wotembereredwa. 18. Kupatula iye amene
amamvetsera mwakuba, iye amatsatiridwa ndi malawi a
moto.

19. Ife tidatambasula dziko lapansi ndi kuikamo mapiri
ndipo tameletsa mu ilo zinthu zosiyanasiyana chilichonse
chili ndi muyeso wake. 20. Ndipo takupatsani mu ilo

njira zopezela chakudya chanu ndi cha izo zimene inu
simungathe kuzidyetsa.

21. Palibe chilichonse, chimene nkhokwe yake siili ndi Ife
ndipo sititumiza kupatula m'muyeso wodziwika. 22. Ndipo
Ife timatumiza mphepo yobereketsa ndipo timatsitsa
madzi kuchokera kumwamba ndipo timakupatsani kuti
mumwe; ndipo inu si ndinu osunga nkhokwe zake.

23. Ndipo, ndithudi, Ife ndife amene timapereka moyo
ndi imfa ndipo zinthu zonse ndi zathu. 24. Ndipo, ndithudi,
Ife timadziwa onse amene adalipo kale inu musanadze
ndipo timadziwa mibadwo yanu yatsopano ndi iwo amene
adzadza m'tsogolo. 25. Ndipo, ndithudi, Ambuye wako
adzasonkhanitsa onse pamodzi. Zoonadi Iye ndi Wanzeru
ndi Wodziwa chilichonse.

26. Ndipo, ndithudi, Ife tidamulenga munthu kuchokera
ku dothi lotulutsa mawu, losinthidwa m'matope akuda
osalala. 27. Tidapanga mtundu wa majini poyamba
kuchokera ku mphepo ya moto.

28. Ndipo pamene Ambuye wako adati kwa angelo, "Ine
ndilenga munthu kuchokera ku dothi lotulutsa mawu
losinthidwa matope akuda osalala." 29. "Motero ndikatha
kumukonza ndi kuuzira mpweya umene ndidalenga
chifukwa cha iye ndipo nonse gwadani kumulambira
iye." 30. Motero Angelo onse adagwada ndi kumulambira.
31. Kupatula Satana adakana kukhala mmodzi mwa olambira.
32. Mulungu adati, "Oh iwe Satana! Kodi ndi chifukwa
chiyani siuli pamodzi ndi olambira?" 33. Satana adati,
"Ine sindingagwadire munthu amene Inu mwamulenga
kuchokera ku dothi lotulutsa mawu losinthidwa matope
akuda osalala."

34. Mulungu adati: "Motero choka kuno chifukwa
ndithudi iwe ndiwe wotembereredwa." 35. Ndipo, ndithudi,
temberero lidzakhala pa iwe mpaka pa tsiku lachiweruzo."
36. Satana adati, "Oh Ambuye wanga! Bandisungani mpaka
patsiku louka kwa akufa." 37. Mulungu adati, "Ndithudi iwe
uli m'gulu la anthu amene apatsidwa nthawi." 38. "Mpaka pa
nthawi ya tsiku lotsimikizika."

39. Satana adati, "Oh Ambuye wanga! Popeza Inuyo
mwandisocheretsa ine, ndithudi, ndidzawasalalitsira njira
yautchimo anthu onse padziko lapansi, ndithudi onse
ndidzawasocheretsa. 40. Kupatula akapolo anu osankhidwa
amene ali pakati pawo."

41. Mulungu adati, "Imeneyi ndiyo njira imene idzalondola
mwachindunji kwa Ine." 42. "Ndithudi iwe siudzakhala
ndi mphamvu pa akapolo anga, kupatula anthu ochita
zoipa amene amakutsatira iweyo." 43. "Ndipo, ndithudi,
Gahena ndi malo olonjezedwa kwa iwo onse." 44. "Iyo ili
ndi makomo asanu ndi awiri, ndipo chipata chilichonse
chidzakhala ndi anthu ake olowapo."

45. "Ndithudi! Onse oopa Mulungu adzakhala m'kati
mwa minda ndi m'kati mwa a kasupe." 46. "Lowanimo
mwamtendere mopanda mavuto." 47. "Ndipo Ife
tidzachotsa m'mitima yawo mkwiyo uliwonse kuti akhoza
kukhala pachibale ndi kupumula m'mipando yawofowofo
moyang'anizana." 48. "Ndipo iwo sadzatopa kumeneko
ndipo sadzafunsidwa kuti achoke ku Paradiso." 49. Auze
akapolo anga kuti ndithudi Ine ndimakhululukira ndipo
ndine wachisoni. 50. Ndiponso kuti chilango changa,
ndithudi, ndi chilango chowawa koposa.

51. Auze za alendo a Abrahamu. 52. Pamene iwo adadza kwa

iye ndi kumuuza kuti, “Mtendere ukhale kwa iwe.’ Koma
iye adawayankha kuti, “Ndili ndi mantha ndi inu.” 53. Iwo
adati, “Usaope! Ife tadza kwa iwe ndi nkhani yabwino ya
mwana wamwamuna amene adzakhala wodziwa zambiri.”
54. Iye adati, “Kodi inu muli kudzandiuza nkhani yabwino
pamene ine nditakalamba kale? “Kodi nkhani yanu ndi
yotani?” 55. Iwo adati, “Ife tili kukuuza nkhani yabwinoyi
mwachoonadi. Kotero usakhale wotaya mtima.” 56. Iye
adati, “Ndani amene angataye mtima ndi chifundo cha
Mulungu, kupatula osochera?”

57. Iye adatinso, “Kodi cholinga chanu ndi chiyani, inu
otumidwa?” 58. Iwo adati, “Ife tatumidwa kwa anthu oipa.”
59. “Onse kupatula anthu otsatira Loti okha. Ife, ndithudi,
tidzawapulumutsa iwo okha.” 60. “Kupatula mkazi wake
amene ife talamulidwa kuti akhalire m’mbuyo pamodzi ndi
iwo amene anali kukhalira m’mbuyo.”

61. Ndipo pamene a Kazembe athu adadza ku nyumba
ya Loti. 62. Loti adati, “Ndithudi inu ndinu anthu omwe
sindikudziwani.” 63. Iwo adati, “Iyayi. Ife takubweretsera
iweyo zinthu zimene iwo anali kukayika.” 64. “Ndipo Ife
tadza ndi choonadi kwa iwe ndipo, ndithudi, ife ndife
onena zoona.” 65. “Motero choka ndi abale ako pakati pa
usiku, iwe uziyenda pambuyo pawo ndipo usalole wina
aliyense kuti atembenuke. Kapita kumene walamulidwa
kupita.” 66. Ndipo tidamuuza lamulo ili kuti mizu ya iwo
idzazulidwa m’mawa.

67. Ndipo anthu a mu Mzinda adadza ali osangala.
68. Iye adati, “Ndithudi! Awa ndi alendo anga motero
musandichititse manyazi ayi.” 69. “Opani Mulungu ndipo
musandipangitse manyazi.” 70. Iwo adati, “Kodi ife

sitidakuletse kuti uzichereza alendo?” 71. Iye adati, “Awa ndi
ana anga a aakazi; akwatireni ngati inu mufunadi kutero.”
72. Ndithudi pali moyo wako! Iwo chifukwa chakuledzera
anali kuyenda mwakhungu. 73. Ndipo chilango chidawapeza
pamene dzuwa linkatuluka. 74. Ndipo Ife tidaononga
(mizinda yawo) zapansi kukhala pamwamba ndipo
tidawagwetsera mvula ya miyala ya moto. 75. Ndithudi! Mu
izi muli zizindikiro kwa anthu omvetsa. 76. Ndipo, ndithudi,
iyo ili m’mphepete mwa msewu umene umapitidwa.
77. Ndithudi! Mu izi muli zizindikiro kwa anthu okhulupirira.
78. Ngakhale anthu okhala m’nkhalango nawonso anali
ochimwa. 79. Motero Ife tidawalanga. Ndipo iwo ali pamalo
poonekera. 80. Ndipo, ndithudi, anthu a ku Hijr adakana
Atumwi. 81. Ndipo Ife tidawapatsa zizindikiro zathu
koma iwo adazikana. 82. Ndipo iwo anali kukumba mapiri
kukhala nyumba zawo ndipo anali kukhala mosaopa.
83. Phokoso la chilango lidafika kwa iwo m’mawa. 84. Ndipo
sizidawathandize zonse zimene anali kuchita.
85. Ndipo Ife sitidalenge kumwamba ndi dziko
lapansi ndi zonse zimene zili pakati pawo kupatula ndi
choonadi. Ndithudi popanda chikayiko tsiku lachiweruzo
lidzadza; kotero akhululukireni, kukhululuka kwabwino.
86. Ndithudi Ambuye wako ndi Namalenga ndi wodziwa
zinthu zonse.
87. Ndipo, ndithudi, Ife tidakupatsa mavesi asanu
ndi awiri amene amanenedwa kawirikawiri ndi Korani
yolemekezeka. 88. Usamayang’ane mwanjiru zinthu zokoma
zimene tawapatsa ena a iwo kapena kumamva chisoni pa
izo. Ndipo onetsani chifundo kwa anthu okhulupirira.
89. Ndipo Nena, “Ine ndine Mchenjezi” 90. Monga

tidatumiza kwa amene amagawanitsa. 91. Amene apanga
Buku la Korani kukhala magawo awiri. 92. Kotero, pali
Ambuye wako, tidzawafunsa. 93. Pa zonse zimene anali
kuchita.

94. Motero lalikira poyera zonse zimene walamulidwa,
ndipo choka pakati pa osakhulupirira. 95. Ndithudi Ife
tidzakuteteza kwa onyoza. 96. Iwo amene amatumikira
mulungu wina kuonjezera pa Mulungu weniweni iwowo
adzadziwa. 97. Ndithudi Ife tili kudziwa kuti zimakupweteka
mumtima mwako zinthu zimene amanena. 98. Motero
lemekeza Ambuye wako ndipo khala mmodzi wa iwo
amene amagwada pomulemekeza Iye. 99. Ndipo pembedza
Ambuye wako mpaka pamene ola lotsimikizidwa likupeza.

Sura 16 • An-Nahl

# Al-Nahl

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Chiweruzo cha Mulungu chidzabwera, ndipo kotero
musachifulumizitse. Kulemekezeka ndi kuyamikidwa
kukhale kwa Iye kuposa zonse zimene akumufanizira.
2. Iye amatsitsa angelo ndi mawu ake amalamulo kwa akapolo
ake amene wawafuna ndikuwauza kuti muwachenjeze iwo
kuti, "Kulibe Mulungu wina koma Ine ndekha. Kotero
ndiopeni Ine." 3. Iye adalenga kumwamba ndi dziko lapansi
mwachoonadi. Iye akhale kutali ndi zimene akumufanizira
nazo.

4. Iye ndiye adalenga munthu kuchokera ku dontho la
umuna ndi la ukazi ndipo taonani iye amatsutsa poyera.
5. Iye adakulengerani nyama ndipo mu izo mumapeza
zofunda ndi zithandizo zina ndiponso nyamazo mumadya.
6. Ndipo mumanyadira pamene mumazisaka kudza nazo
ku nyumba kwanu madzulo ndi pamene mumapita nazo
kuubusa kukazidyetsa m'mawa. 7. Ndipo izo zimanyamula
katundu wanu wolemera kupita kumalo kumene inu
simutha kukafikako kupatula movutikira. Ndithudi
Ambuye wanu ndi Mwini chifundo ndi Mwini chisoni
chosatha. 8. Ndipo adalenga akavalo, abulu ndi mahatchi
kuti muzikwera ndi kukongoletsa. Ndipo adalenganso zina
zimene simuzidziwa.
9. Zili kwa Mulungu kusonyeza njira yoyenera, koma pali
njira zina zopatuka ndipo Iye akadafuna akadakutsogolerani
nonse.
10. Iye ndiye amene amatsitsa madzi kuchokera ku
mitambo omwe inu mumamwa ndipo amameretsa mitengo
imene mumadyetsa ziweto. 11. Kudzera m'menemu, Iye
amakumeretserani mbewu ndi mitengo ya mafuta, mitengo
ya tende ndi mphesa ndiponso zipatso zina. Ndithudi! Mu
ichi muli chizindikiro kwa anthu a maganizo abwino.
12. Ndipo adakupeputsirani usiku ndi usana, dzuwa
ndi mwezi ndi nyenyezi, mwalamulo lake. Ndithudi
mu zimenezi muli zizindikiro kwa anthu ozindikira.
13. Ndipo chilichonse chimene adakulengerani padziko
lapansi adachilenga cha mitundu yosiyanasiyana. Kotero
chilichonse chili ndi chisonyezo kwa anthu omwe
amasangalala ndi matamando a Mulungu.
14. Iye ndiye amene adakupeputsirani nyanja kuti inu

muzidya nyama yaiwisi kuchokera mu iyo ndi kutulutsa
zovala zokongola zimene mumavala. Ndipo mumaona
ngalawa zili kuyenda pa nyanja. Adalenga zonsezi kuti
muzipezamo zokoma zake ndi kuti muzikhala othokoza.
15. Ndipo Iye adakhazikitsa mapiri padziko lapansi kuti
lisagwedezeke pamodzi ndi inu, mitsinje ndi misewu kuti
mutsogozedwe munjira zabwino. 16. Ndi zizindikiro zina
zokutsogolerani, nyenyezi nazonso anthu amatsogozedwa
nazo.
17. Kodi Iye amene amalenga angafanane ndi Iye amene
salenga? Kodi inu simungakumbukire? 18. Ngati inu
mutawerenga zokoma za Mulungu simungakwaniritse
kuziwerenga. Ndithudi! Mulungu ndi wokhululukira ndi
Mwini chisoni chosatha. 19. Ndipo Mulungu amadziwa
zonse zimene mumabisa ndi zimene mumaonetsera.
20. Koma milungu yabodza imene anthu osakhulupirira
amapembedza m'malo mwa Mulungu, siinalenge china
chilichonse ayi chifukwa nayonso ndi yolengedwa. 21. Iyo
ndi yakufa, si yamoyo ayi ndiponso iyo siidziwa nthawi
imene idzaukitsidwe. 22. Mulungu wanu ndi Mulungu
mmodzi yekha. Koma iwo amene sakhulupirira za m'moyo
umene uli nkudza, mitima yawo imakana ndipo iwo ndi
odzikweza. 23. Mosakayika, ndithudi, Mulungu amadziwa
zonse zimene iwo amabisa ndi zimene amaonetsera.
Ndithudi, Iye sakonda anthu odzikweza.
24. Pamene amafunsidwa kuti, "Kodi Ambuye wanu
wavumbulutsa zotani?" Iwo amati, "Nkhani zopeka za
anthu a kalekale." 25. Iwo adzanyamula katundu wawo
okwanira pa tsiku la kuuka kwa akufa pamodzi ndi katundu

wa iwo amene adawasocheretsa mu umbuli. Ndithudi
zoipa ndi zimene akusenza.
26. Iwo amene adalipo kale adakonza chiwembu koma
Mulungu adaphwanya nyumba zawo kuyambira pa maziko
ake ndipo denga lidawagwera kuchokera pamwamba pawo
ndipo chilango chidadza pa iwo kuchokera ku mbali imene
iwo sanali kuganiza. 27. Ndipo patsiku la kuuka kwa akufa
Iye adzawachititsa manyazi ndipo adzati, “Zili kuti zimene
munkandifanizira nazo, zimene inu mumakangana ndi
Aneneri chifukwa cha izo?” Iwo amene adapatsidwa nzeru
adzati, “Ndithudi! Zochititsa manyazi ndiponso zoipa
ziwagwera lero lino anthu osakhulupirira.”
28. Iwo amene angelo amawatenga ali odzipondereza
okha, adzagonja mwachinyengo ponena kuti, “Ife sitinali
kuchita choipa.” Angelo adzati, “Indedi! Ndithudi Mulungu
amadziwa zonse zimene munali kuchita.” 29. “Kotero lowani
m’zipata za Gahena, kumeneko mudzakhalako mpaka
kalekale. Ndithudi ndi oipa malo a anthu odzikweza.”
30. Ndipo kwa anthu oopa zidzanenedwa kuti, “Kodi
Ambuye wanu adavumbulutsa zotani?” Iwo adzati,
“Zabwino.” Mphotho yabwino idzakhala ya iwo amene
adachita ntchito zabwino m’moyo uno. Koma nyumba
yabwino kwambiri ndi mphotho ya moyo umene uli
nkudza ndi mtendere wabwino ndiponso nyumba ya
anthu oopa Mulungu. 31. Iwo adzalowa m’minda yamuyaya
ndipo mitsinje idzayenda pansi pake. Iwo, kumeneko,
adzapeza zonse zimene adzazifuna. Mmenemu ndi mmene
Mulungu adzawalipirire anthu oopa Mulungu. 32. Iwo
amene angelo amatenga miyoyo yawo ali kuchita zabwino,
Angelo adzanena kuti, “Mtendere ukhale kwa inu. Lowani

mu Paradiso, chifukwa cha ntchito zabwino zimene
munkachita.”
33. Kodi iwo akudikira kuti angelo adze kwa iwo kapena
kuti libwere lamulo kuchokera kwa Mulungu wanu?
Chomwecho ndicho adachita iwo amene adalipo kale.
Mulungu sadawapondereze koma iwo adadzipondereza
okha. 34. Ndipo mavuto adawapeza iwo chifukwa cha
zimene adachita ndipo adawazungulira masautso a zinthu
zimene iwo amazikana.
35. Ndipo anthu opembedza mafano amati, “Mulungu
akadafuna, ife kapena makolo athu, sitikadapembedza
milungu ina yoonjezera pa Mulungu weniweni ayi ndiponso
ife sitikadaletsa china chilichonse opanda chilolezo chake.”
Mmenemo ndimo adachitira anthu amene adalipo kale
iwo asanadze. Kodi Atumwi adapatsidwa china kupatula
kupereka Uthenga momveka?
36. Ndithudi! Ife tidatumiza Mtumwi pakati pa mtundu
uliwonse amene amanena kuti, “Pembedzani Mulungu
ndipo mupewe milungu yabodza.” Pakati pawo padali ena
amene Mulungu adawatsogolera ndi ena mwa iwo amene
kusochera kwawo kudali koyenera. Yendani pa dziko
lonse lapansi ndipo mukaone kuti adali bwanji mapeto a
anthu osakhulupirira. 37. Ngati iwe ufunitsitsa kuti iwo
atsogozedwe, ndithudi, Mulungu satsogolera amene
wamusocheretsa. Ndipo iwo sadzapeza owathandiza.
38. Iwo adalumbira mwamphamvu M’dzina la Mulungu
kuti, “Mulungu sadzaukitsa munthu wakufa.” Inde, ndi
lonjezo la Mulungu loona ndipo lidzakwaniritsidwa, koma
anthu ambiri sadziwa. 39. Kuti Iye adzawaonetse zoonadi
zimene iwo amatsutsana ndi kuti iwo amene sakhulupirira

adziwe kuti adali onama. 40. Ndithudi liwu lathu pa chinthu
chimene tachifuna ndi lakuti timangonena, “Khala” ndipo
chimakhala.

41. Ndi iwo amene adasamuka ndi cholinga
chokondweretsa Mulungu pambuyo poponderezedwa, Ife,
ndithudi, tidzawakhazika padziko mwamtendere. Koma
malipiro a tsiku lachiweruzo adzakhala aakulu kwambiri
iwo akadadziwa. 42. Iwo amene adapirira ndipo adaika
chikhulupiriro mwa Ambuye wawo.

43. Iwe usanadze Ife sitidatumizepo, ena koma amuna
amene tidawapatsa chivumbulutso chathu. Kotero afunse
iwo odziwa mawu a Mulungu ngati iwe siukudziwa.
44. Ndi zizindikiro zooneka ndiponso mabuku opatulika,
Ife tavumbulutsa kwa iwe chikumbutso kuti ulalikire
anthu zonse zimene zatumizidwa kwa iwo ndi kuti akhoza
kulingirira.

45. Kodi iwo amene amakonza chiwembu ndi
odzikhulupirira kuti Mulungu sangawakwirire m’nthaka
kapena kuti chilango sichingagwe pa iwo kuchokera ku
mbali imene sali kuiyembekezera? 46. Kapena iwo ali ndi
chikhulupiriro chakuti Iye sadzawagwira iwo m’maulendo
awo pamene sangathe kuthawa? 47. Kapena kuti Iye
sangawapatse chionongeko cha pang’onopang’ono?
Ndithudi Ambuye wako ndiye Mwini chifundo ndi Mwini
chisoni chosatha.

48. Kodi iwo sakuziona zinthu zimene Mulungu adalenga
mmene zimagwetsera mithunzi yake kumbali ya dzanja
lamanja ndi ku dzanja lamanzere, kumulambira Mulungu
modzichepetsa? 49. Ndipo kwa Mulungu zimagwada zinthu
zonse za mlengalenga ndi za padziko lapansi ndi zonse za

moyo ndi angelo, ndipo sizidzikweza. 50. Izo zimaopa
Ambuye wawo amene ali pamwamba pawo ndipo zimachita
monga momwe zalamulidwira.
51. Mulungu adati, “Inu musapembedze milungu iwiri ayi.
Ndithudi Iye ndi Mulungu mmodzi yekha. Kotero ndiopeni
Ine.” 52. Ndipo zonse zimene zili mlengalenga ndi m’dziko
lapansi ndi zake ndipo Iye yekha ayenera kupembedzedwa
basi. Kodi inu mudzaopa wina wake wosati Mulungu?
53. Ndipo zokoma zonse zimene mumalandira
zimachokera kwa Mulungu. Ndipo pamene mavuto
akupezani, inu mumapempha chithandizo kwa Iye.
54. Koma Iye akakuchotserani inu mavuto, taonani! Ena
mwa inu mumaphatikiza Ambuye wanu ndi mafano
mukamapembedza. 55. Motero iwo amakana zimene
tawapatsa! Choncho basangalalani pang’ono koma
posachedwapa mudzadziwa choonadi. 56. Ndipo iwo
amapereka gawo lina la zinthu zimene tawapatsa ku zinthu
zimene iwo sazidziwa. Pali Mulungu, inu mudzafunsidwa
zinthu zonse zabodza zimene mumapeka!
57. Ndipo iwo amamupatsa Mulungu ana aakazi.
Ayeretsedwe Ambuye ndipo Iye akhale pamwamba pa
zonse zimene amaziphatikiza ndi Iye ndi zimene iwo
amafuna. 58. Ndipo pamene kubadwa kwa mwana wamkazi
kumemezedwa kwa wina wa iwo, nkhope yake imada
ndipo amadzadzidwa ndi chisoni. 59. Iye amadzibisa kuti
asaonane ndi anthu ake chifukwa cha nkhani yoipa imene
wauzidwa. Kodi mwanayu akhale naye ndi manyazi kapena
kuti akamukwirire m’nthaka? Ndithudi chiweruzo chawo
ndi choipa kwambiri. 60. Iwo amene sakhulupirira zatsiku
lachiweruzo ali ndi mbiri yoipa pamene Mulungu ali ndi

mbiri yaulemerero. Iye ndiye Mwini mphamvu zonse
ndiponso ndi Wanzeru.
61. Akadakhala kuti Mulungu anali kulanga anthu msanga
chifukwa cha zoipa zawo, palibe cholengedwa ndi chimodzi
chomwe chimene Iye akadachisiya ndi moyo. Koma Iye
amawasunga mpaka tsiku lokhazikitsidwa, ndipo ngati
nthawi yawo ikwana, ngakhale ndi kamphindi kochepa,
iwo sangaichedwetse kapena kuifulumizitsa.
62. Iwo amamupatsa Mulungu zinthu zimene iwo amazida,
ndipo malirime awo amanena bodza lakuti mphotho
yabwino ili kuwayembekezera. Mosakayika kwawo ndi
kumoto ndipo iwo adzakhala oyamba kuponyedwako
ndipo adzasiyidwa m'menemo osasamalidwa.
63. Pali Mulungu, ndithudi, Ife tidatumiza Atumwi ena,
ku mibadwo ina, iwe usanadze. Koma Satana adasandutsa
ntchito zawo zoipa kuti zikhale zabwino kwa iwo. Motero
Satana ndiye bwenzi lawo. Chawo chidzakhala chilango
chowawa zedi. 64. Ndipo Ife sitinavumbulutse Buku kwa
iwe kupatula kuti iwe uwauze anthu poyera choonadi cha
zinthu zimene ali kukangana ndiponso ngati chilangizo ndi
dalitso kwa anthu okhulupirira moonadi.
65. Mulungu amatsitsa madzi kuchokera ku mtambo ndipo
Iye amadzutsira nthaka pambuyo poti idafa. Ndithudi mu
zimenezi muli zizindikiro kwa anthu akumva.
66. Ndithudi! Mu nyama muli phunziro kwa inu. Ife
timakupatsani kuti muzimwa zina mwa zomwe zili
m'mimba mwake kuchokera pakati pa ndowe ndi magazi.
Mkaka wabwino, chakumwa chabwino kwambiri kwa iwo
amene amamwa. 67. Ndipo kuchokera ku zipatso za mitengo
ya tende ndi mitengo ya mphesa, inu mumapanga zakumwa

zoledzeretsa ndiponso chakudya chabwino. Ndithudi mu
zimenezi muli zizindikiro kwa anthu amene ali ndi nzeru.
68. Ambuye wako adauza njuchi kuti, “Mangani nyumba
zanu m’mapiri, m’mitengo ndi m’ming’oma imene anthu
amakonza.” 69. “Ndipo idyani zipatso za mitundu yonse,
ndipo yendani m’njira za Ambuye wanu mosavutika.”
Kuchokera m’mimba mwa njuchi, mumatuluka zakumwa
zamitundu yosiyanasiyana ndipo m’menemo muli
mankhwala ochiza anthu. Ndithudi mu izi muli zizindikiro
kwa iwo amene amalingilira.
70. Mulungu ndiye amene adakulengani inu ndipo
adzakuphani. Ndipo ena a inu amakalamba koti sangathe
kuzidziwa zinthu zimene anali kuzidziwa kale. Ndithudi!
Mulungu amadziwa chilichonse ndiponso ali ndi mphamvu
zonse.
71. Ndipo Mulungu wawalemekeza ena a inu kuposa ena
powapatsa chuma chambiri. Ndipo iwo amene apatsidwa
zambiri sadzapereka ngakhale zitavuta chotani chuma
chawo kwa akapolo awo kuti mwina akhoza kufanana pa
chuma. Kodi iwo amakana zokoma za Mulungu?
72. Ndipo Mulungu wakupatsani akazi kuchoka pakati
panu ndipo kudzera mwa iwo wakupatsani ana aamuna ndi
zidzukulu ndipo Iye wakupatsani zinthu zabwino. Kodi
iwo tsopano adzakhulupirira mu zinthu zabodza ndikukana
ubwino wa Mulungu? 73. Ndipo iwo amapembedza mafano
mowonjezera pa Mulungu amene sangathe kuwapatsa
chithandizo chilichonse kuchokera kumwamba kapena
padziko lapansi. 74. Motero musafanizire wina aliyense
ndi Mulungu. Ndithudi Mulungu amadziwa pamene inu
simudziwa chilichonse.

75. Mulungu akupereka fanizo la kapolo amene ali
mu ulamuliro wa bwana wake amene sangathe kuchita
chilichonse ndi munthu wina, amene tamupatsa zinthu
zabwino ndipo iye amapereka kuchokera ku zimene
wapatsidwa mwamseri ndiponso moonekera. Kodi iwo
angafanane? Kuyamikidwa konse kukhale kwa Mulungu,
koma ambiri a iwo sazindikira.
76. Ndipo Mulungu ali kuperekanso fanizo la anthu ena
awiri, mmodzi wa iwo wosayankhula amene sangathe
kuchita chilichonse, ndi wosathandiza Ambuye wake
chifukwa kulikonse kumene amamutuma iye sabweretsa
chabwino. Kodi iyeyu ndi wofanana ndi iye amene
amalamula mwachilungamo ndipo ali m'njira yoyenera?
77. Zinsinsi zimene zili mlengalenga ndi pa dziko lapansi
zonse ndi za Mulungu. Ntchito yokhudza ola lomaliza
idzagwiridwa mu nthawi ngati kuphethira kwa diso kapena
kufulumira koposerapo apa. Ndithudi Mulungu amatha
kuchita chilichonse.
78. Ndipo Mulungu adakutulutsani kuchokera m'mimba
mwa amayi anu muli osadziwa china chilichonse ndipo
adakupatsani makutu, maso, ndi mitima kuti muzithokoza.
79. Kodi iwo saona mbalame zomwe zimauluka
mlengalenga? Palibe wina amene amazigwira kuti zisagwe
pansi koma Mulungu yekha. Ndithudi mu ichi muli
zizindikiro kwa anthu okhulupirira. 80. Ndipo Mulungu
wakupangirani nyumba zanu kuti muzikhalamo ndipo
wakupangirani nyumba kuchokera kuzikopa za nyama,
zomwe mumaona kuti zimakupepukirani ponyamula
ndikumakhala pamodzi ndi ubweya umene mumakonzera
zinthu zina zofunika.

81. Ndipo Mulungu wakupangirani kuchokera ku zinthu
zimene adalenga mthunzi ndipo wakupangirani malo
othawirako m'mapiri ndipo Iye wakupangiraninso zovala
kuti zizikutetezani kukatentha ndi zovala zokutetezani
ngati chishango nthawi ya nkhondo. Mmenemo ndimo
mmene amakwaniritsira ubwino wake pa inu kuti mukhale
odzipereka mwahifuniro chake. 82. Koma ngati iwo
samvera, udindo wako ndi kufikitsa uthenga moonekera.
83. Iwo amazindikira ubwino wa Mulungu komabe
amaukana ndipo ambiri a iwo ndi anthu osakhulupirira.

84. Ndipo patsiku limene Ife tidzadzutsa mboni
kuchokera ku mtundu uliwonse, iwo amene sanakhulupirire
sadzapatsidwa mwayi. 85. Ndipo pamene ochita zoipa
adzaona chilango, mavuto awo sadzachepetsedwa ndipo
sadzapatsidwa mpumulo.

86. Ndipo anthu opembedza mafano akadzaona mafano
awo, iwo adzati, "Oh Ambuye wathu! Awa ndi mafano
athu amene tinali kupembedza kuonjezera pa inu." Koma
mafano awo adzayankha opembedzawo nati, "Ndithudi!
Inu ndinu abodza." 87. Patsiku limeneli, iwo adzaonetsera
poyera kugonja kwawo kwa Mulungu ndipo mafano awo
onse adzawathawira iwo. 88. Kwa iwo amene sadakhulupirire
ndipo adatsekereza anzawo kutsatira njira ya Mulungu, Ife
tidzawaonjezera chilango kuonjezera pa chilango china,
chifukwa cha ntchito zawo zoipa zimene anali kufalitsa.

89. Ndipo patsikulo tidzadzutsa kuchokera ku mtundu
uliwonse amene adzawachitira umboni wochokera pakati
pawo. Ndipo tidzakubweretsa iwe kukhala mboni ya anthu
awa. Ndipo takuvumbulutsira Buku lolongosola zonse,

chilangizo, madalitso ndi nkhani yabwino kwa omwe
amagonjera Mulungu.
90. Ndithudi Mulungu amalamulira chilungamo, kupirira
pogwira ntchito ya Mulungu, ubwino ndi kupereka chaulere
kwa abale. Ndipo amaletsa ntchito zoipa, zonyansa ndi
kuponderezana. Iye ali kukuchenjezani kuti mukhale
okumbukira.
91. Kwaniritsani pangano la Mulungu mukalonjeza ndipo
musaphwanye malonjezo anu mutatsimikiza. Ndithudi inu
mwamupanga Mulungu kukhala mboni yanu yodalirika.
Ndithudi Mulungu amadziwa zonse zimene mumachita.
92. Musakhale ngati mkazi amene wadula ulusi wa nsalu
imene amasoka italimba polumbira mwachinyengo pakati
panu kuti mwina gulu lina lingakhale lopambana kuposa
gulu linzake. Ndithudi mu ichi Mulungu amakuyesani.
Ndipo patsiku la kuuka kwa akufa, Iye adzakuululirani
zoona zokhazokha za izo zimene munali kusemphana
maganizo.
93. Ndipo Mulungu akadafuna, akadakupangani inu
kuti mukhale mtundu umodzi. Koma Iye amasocheretsa
amene Iye wamufuna ndipo amamutsogolera Iye amene
wamufuna. Ndithudi inu mudzafunsidwa za ntchito zanu
zonse zimene munali kuchita.
94. Musasandutse kulumbira kwanu kukhala chinyengo
pakati panu chifukwa mwina phazi lingaterere litakhazikika
ndipo inu mungalawe zoipa chifukwa chakutsekereza njira
ya Mulungu ndipo chanu chidzakhala chilango chachikulu.
95. Musagulitse lonjezo la Mulungu ndi mtengo wochepa.
Ndithudi zinthu zimene zili kwa Mulungu ndi zabwino inu
mukadadziwa.

96. Zinthu zimene zili ndi inu ndi zakutha koma zimene zili
kwa Mulungu ndi zosatha. Ndithudi Ife tidzalipira anthu
omwe amapirira malipiro abwino kwambiri molingana ndi
zimene anali kuchita. 97. Aliyense amene achita zabwino,
mwamuna kapena mkazi, ndipo ali okhulupirira, ndithudi,
tidzampatsa moyo wabwino ndipo tidzawalipira malipiro
abwino kwambiri molingana ndi zimene ankachita.
98. Motero ukafuna kuwerenga Korani, pempha chitetezo
cha Mulungu kuti akuteteze kwa Satana wotembereredwa.
99. Ndithudi! Satana alibe mphamvu pa anthu okhulupirira
amene amaika chikhulupiliro chawo mwa Ambuye wawo.
100. Mphamvu zake zili pa okhawo amene amapalana naye
ubwenzi, ndiponso iwo amene amapembedza milungu ina
yoonjezera pa Mulungu weniweni.
101. Ndipo pamene Ife tisintha Vesi m'malo mwa
linzake, Mulungu yekha amadziwa kwambiri zimene
akuvumbulutsa. Iwo amati, "Iwe ndiwe wabodza." Iyayi
koma ambiri mwa iwo sadziwa. 102. Nena, "Ndi Mzimu
Woyera umene wabweretsa chivumbulutso kuchokera
kwa Ambuye wako mwachoonadi, ndi cholinga choti
chiwalimbikitse anthu amene amakhulupirira, ndi
malangizo ndiponso nkhani yabwino kwa Asilamu."
103. Ndithudi Ife tikudziwa kuti iwo amanena kuti, "Ndi
munthu amene akumuphunzitsa iye." Koma munthu
amene amamuganizira, kuti ndiye amene anamuphunzitsa
amayankhula chiyankhulo cha chilendo pamene Korani iyi
ndi chiyankhulo cha Chiarabu chomveka. 104. Ndithudi!
Iwo amene sakhulupirira mawu a Mulungu, Mulungu
sadzawatsogolera ndipo iwo adzapeza chilango chowawa.

105. Ndithudi ndi okhawo amene sakukhulupirira mavesi a
Mulungu amene amapeka bodza ndipo iwo ndi abodza.
106. Aliyense amene sakhulupirira Mulungu pambuyo
pokhulupirira kupatula amene wakakamizidwa koma
mtima wake uli wokhazikika ndi chikhulupiriro, koma iwo
amene ayamba kusakhulupirira mu mtima mwawo, mkwiyo
wochokera kwa Mulungu udzadza pa iwo ndipo adzapeza
chilango chachikulu. 107. Ichi ndi chifukwa chakuti anthu
otero adakonda moyo wa padziko lapansi kwambiri kuposa
moyo umene uli nkudza. Ndipo Mulungu satsogolera anthu
osakhulupirira. 108. Amenewa ndiwo amene mitima yawo,
makutu awo ndi maso awo atsekedwa ndi Mulungu ndipo
ndi osamva ayi. 109. Palibe chikayiko kuti iwo, m'moyo
umene uli nkudza, sadzapeza chilichonse ndipo adzakhala
olephera.
110. Ndipo, ndithudi, Ambuye wako, kwa iwo amene
adasamuka kwawo pambuyo povutitsidwa ndipo apitirira
kumenya nkhondo ndi kupirira, ndithudi, Ambuye wako,
pambuyo pa zimenezo ndi Wokhululukira kwambiri
ndiponso Wachisoni. 111. Pa tsiku limene munthu aliyense
adzadza kudzadzidandaulira yekha, ndipo aliyense
adzalandira dipo lolingana ndi ntchito zake ndipo iwo
sadzaponderezedwa ayi.
112. Ndipo Mulungu wapereka chitsanzo cha Mzinda
umene udali wabata ndi wamtendere, chakudya chake
chidali chambiri chimene chimachokera kumbali
zosiyanasiyana koma anthu ake adakana zokoma za
Mulungu. Kotero Mulungu adaulawitsa Mzindawo vuto
la njala ndi mantha chifukwa cha zimene iwo amachita.
113. Ndithudi! Kudadza kwa iwo Mtumwi wa mtundu

wawo koma iwo adamukana. Choncho chilango chathu
chidawapeza iwo ali kuchita zoipa.
114. Motero idyani zinthu zabwino ndi zololedwa zimene
Mulungu wakupatsani inu. Ndipo thokozani chisomo
cha Mulungu ngati ndiye yekha amene mumapembedza.
115. Iye wakuletsani kudya zinthu zofa zokha, liwende,
nyama ya nkhumba, ndiponso nyama iliyonse imene
yaphedwa m'dzina la mulungu wina wosati Mulungu
mmodzi yekha. Koma ngati wina akakamizidwa kudya
zina za izi, osati mofuna yekha kapena mofuna kuphwanya
malamulo, ndithudi, Mulungu ndi wokhululukira ndi
wachifundo chosatha.
116. Ndipo musanene bodza ndi malirime anu ponena
kuti, "Ichi ndi chololedwa kapena ichi ndi choletsedwa"
ndi cholinga chomupekera Mulungu bodza. Ndithudi
amene akupekera Mulungu bodza sadzapambana.
117. Chisangalalo cha kanthawi kochepa kwambiri koma iwo
adzapeza chilango chowawa.
118. Ife tidawaletsa Ayuda kudya zakudya zimene
takufotokozera kale. Ife sitidawapondereze ayi koma
iwo adadzipondereza okha. 119. Ndipo, ndithudi! Ambuye
wako, kwa anthu amene amachita zoipa mosazindikira
ndi kulapa pambuyo pake ndikuchita zabwino, ndithudi,
Ambuye wako pambuyo pa zimenezo ndi wokhululukira
ndi wachisoni.
120. Ndithudi! Abrahamu adali chitsanzo cha makhalidwe
abwino, wokhulupirika kwa Mulungu ndiponso wangwiro.
Iye sadali mmodzi wa anthu opembedza mafano.
121. Iye adali wothokoza chisomo cha Mulungu ndipo Iye
adamusankha iye ndi kum'tsogolera ku njira yoyenera.

122. Ndipo Ife tidamupatsa zabwino m'moyo uno ndipo
iye, m'moyo umene uli nkudza, adzakhala pakati pa anthu
olungama. 123. Motero Ife tavumbulutsa kwa iwe kuti,
"Tsatira chipembedzo cha Abrahamu amene sanali mmodzi
wopembedza mafano."

124. Tsiku la sabata lidakhazikitsidwira anthu amene
adali kutsutsana pa za tsikuli ndipo ndithudi Ambuye
wako adzaweruza zonse zimene anali kukangana pa tsiku
lachiweruzo.

125. Itanira anthu ku njira ya Ambuye wako mwanzeru ndi
ulaliki wabwino. Tsutsana nawo m'njira yabwino. Ndithudi
Ambuye wako amadziwa bwinobwino onse amene
amasochera ku njira yake, ndiponso Iye amawadziwa
bwino bwino iwo amene atsogozedwa.

126. Ngati inu muli kulanga, langani monga momwe inu
mwalangidwira. Koma ngati mutapirira, zimenezo ndi
zabwino kwa anthu opirira. 127. Khala opirira ndipo kupirira
kwako ndi chifukwa cha Mulungu ndipo usadandaule za
iwo ndiponso usakhale obanika chifukwa cha chiwembu
chawo. 128. Ndithudi Mulungu ali ndi iwo amene amamuopa
Iye ndipo amachita ntchito zabwino.

# Bani Israel

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Ulemerero ukhale kwa Iye amene adayendetsa kapolo
wake nthawi ya usiku kuchoka ku Mzikiti Wolemekezeka
kupita ku Mzikiti wakutali umene malo ake ozungulira
tidawadalitsa; kuti timuonetse zina za zizindikiro zathu.
Ndithudi Iye ndiwakumva ndipo woona zonse.
2. Ndipo Ife tidamupatsa Mose Buku ndipo tidalipanga
ilo kukhala chilangizo cha ana a Israyeli ponena kuti,
“Musasankhe wina aliyense kupatula Ine kukhala
wokutetezani.” 3. Oh inu ana a iwo amene tidawanyamula
pamodzi ndi Nowa! Ndithudi Iye adali kapolo wothokoza
kwambiri.
4. Ife tidavumbulutsa kwa ana a Israyeli, m’Buku
kuti, mosakayika, inu mudzabweretsa chisokonezo
padziko kachiwiri ndipo mudzakhala ankhanza ndi
odzikweza kwambiri!. 5. Ndipo litadza pangano loyamba,
Ife tidzakutumizirani akapolo athu a gulu la nkhondo
ankhongono zedi. Iwo amalowa m’katikati mwa nyumba
zanu. Ndipo linali lonjezo limene linakwaniritsidwa.
6. Titatero tidakupatsani mphamvu powagonjetsa
iwo. Ndipo tidakuonjezerani chuma ndi ana ndipo
tidakupangani kukhala anthu ambiri amphamvu.
7. Ngati inu muchita zabwino, mukudzichitira nokha
ubwinowo, koma ngati muchita zoipa, mukudzichitiranso

nokha. Ndipo pamene pangano lomaliza lidza, Ife tidzalola
adani anu kuti akumvetseni chisoni ndi kulowa mu Mzikiti
wanu monga momwe adaloweramo koyamba ndi kukantha
kwenikweni onse amene adawapeza. 8. Mwina Ambuye
wanu adzakuchitirani chifundo koma ngati inu mubwerera
kuuchimo, nafenso tidzabwezera kukanthani. Ife takonza
Gahena kukhala ndende ya anthu osakhulupirira.

9. Ndithudi Korani ino imatsogolera ku zinthu zabwino
ndipo imawauza anthu okhulupirira, amene amachita
zabwino, kuti adzakhala ndi malipiro aakulu. 10. Ndipo
iwo amene sakhulupirira za tsiku lotsiriza Ife tawakonzera
chilango chowawa.

11. Ndipo munthu amapempha zoipa monga momwe
amapemphera zabwino ndipo munthu ndi wopupuluma.
12. Ndipo tidapanga usiku ndi usana kukhala zizindikiro
zathu ziwiri. Ndipo tidakuta chizindikiro chausiku ndi
mdima pamene tidaika chizindikiro chamasana kukhala
chooneka kuti inu muzifunafuna zabwino zochokera kwa
Ambuye wanu, komanso kuti mudziwe kuchuluka kwa
zaka ndi chiwerengero. Ndipo zinthu zonse tazifotokoza
momveka.

13. Ndipo Ife tidamangirira ntchito za munthu aliyense
pakhosi lake ndipo patsiku lachiweruzo tidzamutulutsira
buku limene adzalipeze lili lotsekulidwa. 14. Werenga Buku
lako. Lero pakwana kuti mzimu wako udziwerengere
wokha zonse zimene unkachita. 15. Aliyense amene achita
zabwino atero podzipulumutsa yekha. Ndipo aliyense
amene achita zoipa, atero podzipweteka yekha. Palibe
amene adzanyamula katundu wa mnzake. Ndipo Ife
sitilanga pokhapokha ngati tatumiza Mtumwi.

16. Ndipo pamene Ife tifuna kuononga Mzinda, poyamba
timatumiza ulamuliro wathu kwa anthu ake opeza bwino.
Ndipo iwo amauphwanya, ndipo motero liwu la chilango
limatsimikiza pa iwo. Ndipo Ife timauononga kwambiri.
17. Kodi ndi mibadwo ingati ya anthu imene taononga
pambuyo pa Nowa? Ambuye wako wakwana kukhala
Wozindikira ndi woona zolakwa za akapolo ake.
18. Aliyense amene afuna chisangalalo cha msanga
Ife timapereka msanga chimene Ife tifuna kwa amene
Ife tamufuna. Ndipo pambuyo pake tamukonzera iye
Gahena, imene adzalowa monyozedwa ndi mokankhidwa.
19. Ndipo yense amene afuna moyo umene uli nkudza,
ndi kumaugwirira ntchito zake molimbika, ndipo ndi
wokhulupirira, amenewo ndi amene ntchito zawo
zidzakhala zoyamikidwa.
20. Ife timapereka kuchokera ku mphatso za Ambuye
wako. Ndipo mphatso za Ambuye wako sizokanizidwa
kwa aliyense. 21. Taona mmene tawalemekezera ena kuposa
anzawo ndipo, ndithudi, moyo umene uli nkudza uli ndi
ulemu wambiri ndipo ndi waukulu poyerekeza.
22. Musasankhe mulungu wina ndi kumuphatikiza ndi
Mulungu weniweni chifukwa mungadzakhale ndi manyazi
ndi wopanda wokuthandizani. 23. Ndipo Ambuye wako
walamula kuti musapembedze wina aliyense koma Iye
yekha. Ndipo kuti muwachitire makolo anu zabwino.
Ngati wina wa iwo kapena onse akalamba ali kukhala nanu,
musawakalipire ayi, koma muziwayankhula ndi mawu
aulemu. 24. Onetsani kudzichepetsa ndi chisoni ndipo
munene kuti, “Ambuye wanga! Achitireni chifundo monga
momwe iwo adandilerera pamene ine ndidali wamng’ono.”

25. Ambuye wanu amadziwa kwambiri zonse zimene zili
m'mitima mwanu. Ngati muli abwino ndithudi Iye ali
wokhululukira kwa anthu amene amadza kwa Iye nthawi
zonse modzichepetsa ndi kulapa.
26. Ndipo apatseni abale anu ndi anthu ovutika gawo lawo
lowayenera ndiponso a paulendo amene avutika. Ndipo
musapereke chuma chanu moononga. 27. Ndithudi anthu
oononga ndi abale a Satana ndipo Satana, kwa Ambuye
wake, ndi wosayamika. 28. Ndipo ngati iwe siuwathandiza
ndipo uli kuyembekezera chisomo chochokera kwa
Ambuye wako, yankhula nawo mwachifundo ndi mawu
oleza.
29. Ndipo musakhale oumira kapena opereka moononga
chifukwa mungadzudzulidwe kapena kukhala osauka
kwambiri. 30. Ndithudi Ambuye wako amapereka zambiri
kwa aliyense amene wamufuna ndipo amanyalapsa.
Ndithudi Iye, kwa akapolo ake, ndi wodziwa ndi woona.
31. Ndipo musawaphe ana anu chifukwa choopa umphawi.
Ife timawapatsa zosowa zawo ndi inu nomwe. Ndithudi
kuwapha iwo ndi tchimo lalikulu. 32. Ndipo musayandikire
chigololo. Ndithudi icho ndi chonyansa ndiponso njira
yoipa.
33. Ndipo musaphe wina aliyense amene Mulungu
waletsa pokhapokha ngati pali chifukwa chololedwa.
Ndipo aliyense amene waphedwa mopanda chilungamo,
Ife tamupatsa m'bale wake mphamvu zobwezera kapena
kukhululuka pa imfa yake. Koma m'bale wakeyo asapyole
muyeso pa kubwezeraku. Ndithudi iye ndi wotetezedwa.
34. Ndipo musachiyandikire chuma cha mwana
wamasiye kupatula ngati muli ndi cholinga chochisamala

mpaka pamene mwini wake adzafike pa msinkhu woti
akhoza kuchisamalira yekha. Ndipo kwaniritsani lonjezo
lililonse. Ndithudi! mudzafunsidwa za lonjezoli. 35. Ndipo
kwaniritsani muyeso pamene muyesa zinthu ndipo yesani
mwachilungamo polinga zinthu pa sikelo. Zimenezo ndizo
zabwino ndipo ndi mapeto abwino kwambiri.

36. Ndipo musatsatire zinthu zimene simuzidziwa.
Ndithudi kumvera kapena kuyang’ana kapenanso
kuganizira kwa mumtima mwa munthu kudzafufuzidwa pa
tsiku lachiweruzo. 37. Ndipo musayende modzitukumula
pa dziko lapansi, ndithudi, inu simungathe kuboola nthaka
ndi kufika kutalika kwa mapiri. 38. Kuipa kwa zonsezi
sikukondweretsa Ambuye wako.

39. Ili ndi gawo la luntha limene Ambuye wako wakuuza
iwe. Ndipo usatumikire mulungu wina kuonjezera pa
Mulungu weniweni chifukwa mwina iwe ungaponyedwe ku
Gahena, modzudzulidwa ndi mokankhidwa.

40. Kodi Ambuye wanu wakusankhirani inu ana aamuna
ndipo wadzisankhira Iye mwini ana aakazi kuchokera
kwa Angelo? Ndithudi! Inu mukuyankhula mawu oopsa.
41. Ndithudi Ife tafotokoza chinthu chilichonse m’Korani
iyi kuti iwo achenjezedwe, koma iyo siili kuonjezera
chilichonse koma kuipidwa. 42. Nena, “Kukadakhala kuti
kuli milungu ina yoonjezera pa Mulungu weniweni, monga
momwe akunenera, iyo ikadapeza njira yoti ikhale pafupi
ndi Mulungu.” 43. Kuyamikidwa ndi kukhala pamwamba,
kukhale kwake! Kuchokera ku bodza lalikulu limene iwo
ali nkunena! 44. Miyamba isanu ndi iwiri, dziko lapansi ndi
zonse zimene zimakhala m’menemo zimamulemekeza Iye
ndipo palibe chinthu chomwe sichimulemekeza Mulungu.

Koma inu simumva mayamiko. Ndithudi Iye ndi woleza
mtima ndipo ndi wokhululukira nthawi zonse.
45. Pamene iwe umawerenga Korani, Ife timaika, pakati
pa iwe ndi iwo amene sakhulupirira za moyo umene uli
nkudza tchingo losaoneka. 46. Ndipo Ife taika zophimba
m'mitima mwawo kuti mwina angaizindikire ndi m'makutu
mwawo kuti asaimvetse. Ndipo pamene iwe utchula
Ambuye wako yekha mu Korani iwo amatembenuka
kuthawa mosangalala.
47. Ife timadziwa kwambiri zimene iwo akumva
ndi pamene amamvetsera kwa iwe. Ndipo pamene
amanong'onezana, taona anthu oipa, amanena kuti: "Inu
mukutsatira munthu wolodzedwa." 48. Taona mmene
akuperekera zitsanzo zokhudza iwe. Motero iwo asochera
ndipo sangathe kupeza njira.
49. Ndipo iwo amati, "Kodi pamene ife tidzasanduka
mafupa ndi zidutswa zopereseka kodi tidzaukitsidwanso
kukhala chilengedwe chatsopano?" 50. Nena, "Khalani
miyala kapena zitsulo." 51. "Kapena cholengedwa china
chimene ndi chachikulu m'mitima mwanu." Iwo adzati,
"Ndani amene adzatibwezeranso?" Nena, "Iye amene
adakulengani poyamba." Ndipo iwo adzapukusa mitu
yawo ndipo kwa iwe adzafunsa kuti, "Kodi zimenezi
zidzachitika liti?" Nena, "Mwina zili pafupi." 52. Pa tsiku
limene Iye adzakuitanani ndipo inu mudzamuyankha ndi
matamando ake ndi kumvera, pamenepo inu mudzaganiza
kuti simudakhale nthawi yaitali koma yochepa.
53. Auze akapolo anga kuti aziyankhula zokhazo zimene
zili zabwino. Ndithudi Satana amafesa chidani pakati pawo.
Ndithudi Satana, kwa munthu, ndi mdani woonekeratu.

54. Ambuye wanu amadziwa kwambiri za inu ndipo ngati
Iye afuna adzakuchitirani chifundo kapena ngati Iye
afuna adzakulangani. Ndipo Ife sitidakutumize iwe kuti
ukhale wowayang’anira iwo ayi. 55. Ambuye wako amadziwa
kwambiri zonse zimene zili kumwamba ndi padziko
lapansi ndipo, ndithudi, Ife tidalemekeza Aneneri ena
kuposa anzawo ndipo kwa Davide, Ife tidamupatsa Buku
la Masalimo.

56. Nena, “Aitaneni onse amene mumadzinyengeza
nawo mowonjezera pa Iye. Iwo alibe mphamvu zochotsa
mavuto anu kapena kuwasintha ndi kupatsa munthu wina.”
57. Iwo amene amawapembedza nawonso amafunafuna
njira yodziyandikiritsira kwa Ambuye wawo, kuti
ndani amene angakhale pafupi kwambiri ndi Mulungu
ndipo amafunafuna mtendere wa Mulungu ndikuopa
chilango chake. Ndithudi chilango cha Ambuye wako ndi
chofuna kuopedwa! 58. Ndipo palibe mzinda umene Ife
sitingauononge kapena kuulanga ndi chilango choopsa
tsiku lachiweruzo lisanadze. Izi zidalembedwa m’Buku.

59. Ndipo palibe chimene chimatiletsa Ife kutumiza
zizindikiro kupatula kuti anthu a mvula zakale
sadazikhulupirire izo. Ndipo kwa anthu a Thamoud,
Ife tidawapatsa ngamira yaikazi kukhala chizindikiro
chooneka ndi maso komabe iwo adaichitira zoipa. Ndipo
Ife sititumiza zizindikiro kupatula ndi cholinga chofuna
kuchenjeza ndi kuwachititsa mantha.

60. Ndipo pamene tidakuuza kuti, “Ndithudi! Ambuye
wako wawazungulira anthu. Ndipo Ife sitidapange
masomphenya amene tidakuonetsa iwe koma kukhala
mayeso kwa anthu chimodzimodzinso mtengo

wotembereredwa umene watchulidwa m'Korani. Ife
timawachenjeza ndi kuwachititsa mantha koma sizili
kuwathandiza koma kuonjezera kusakhulupirira."
61. Ndipo pamene ife tidawauza angelo kuti,
"Mugwadireni Adamu." Onse adamugwadira iye kupatula
Satana. Iye adayankha kuti, "Kodi ine ndimugwadire iye
amene Inu mudamupanga kuchokera ku dothi?" 62. Iye
adati, "Mukumuona! Uyu ndiye amene mwamulemekeza
kuposa ine ndipo ngati inu mundisunga ndi moyo mpaka
patsiku louka kwa akufa, ine ndidzawasokoneza ana ake
kupatula ochepa."
63. Mulungu adati, "Pita, ndipo aliyense wa iwo amene
adzakutsatira, ndithudi, Gahena ndiyo idzakhala malipiro
ake ndipo ndi malipiro okwana." 64. "Ndipo anyengerere
amene ungawathe mwa iwo ndi mawu ako, ndipo menyana
nawo ndi asirikali ako okwera akavalo ndi oyenda pansi,
ndipo gawana nawo chuma ndi ana ndipo alonjeze." Koma
Satana sawalonjeza china chilichonse koma chinyengo.
65. "Ndithudi pa akapolo anga angwiro, iwe siudzakhala
ndi mphamvu ina iliyonse pa iwo yowasokoneza. Ambuye
wako ndi wokwana kukhala Mtetezi."
66. Ambuye wanu ndiye amene amayendetsa zombo pa
nyanja kuti mufunefune zokoma zake. Ndithudi Iye ali
wachisoni ndi inu. 67. Ndipo akakupezani mavuto pamene
muli panyanja, iwo amene mumawapembedza mowonjezera
pa Iye amakuthawirani kupatula Iye yekha. Koma ngati
Iye akupulumutsani kufika pa mtunda, mumatembenuka.
Ndithudi, munthu ndi wamwano.
68. Kodi inu muli ndi chikhulupiriro chakuti Iye
sangakumizeni m'dera lililonse la pamtunda kapena kuti

sangakutumizireni mphepo yamkuntho? Pamenepo inu
simudzapeza wina aliyense wokuthandizani. 69. Kapena inu
mukukhulupirira kuti sangakubwezereninso m’nyanjamo
kachiwiri ndi kukutumizirani mphepo yamkuntho,
ndikukumizani chifukwa chakusakhulupirira kwanu ndipo
kuti inu simudzapeza wokuthandizani polimbana ndi Ife.
70. Ndithudi Ife tawalemekeza ana a Adamu, ndipo Ife
tawanyamula pamtunda ndi pa nyanja ndipo tawapatsa
zinthu zabwino ndiponso tawalemekeza kuposa zina
zimene talenga ndi ulemu wapadera.
71. Ndipo kumbukira tsiku limene tidzaitana mtundu
uliwonse wa anthu pamodzi ndi Atsogoleri awo. Ndipo
yemwe adzapatsidwa Buku lake ku dzanja lamanja
iwo adzawerenga Bukulo mwa chisangalalo ndipo
sadzaponderezedwa ngakhale ndi pang’onong’ono pomwe.
72. Koma iye amene ali wakhungu m’moyo uno adzakhalanso
wakhungu m’moyo umene uli nkudza ndipo adzasochera
kwambiri.
73. Ndithudi iwo adali pafupi kuti akusokoneze ku
zimene takuvumbulutsira iwe kuti utinamizire zina ndipo
zikadatero akadakupala ubwenzi. 74. Ngati Ife tikadapanda
kulimbikitsa chikhulupiriro chako, padatsala pang’ono
kuti uwatsatire. 75. Ndipo zikadatero Ife tikadakulawitsa
chilango chachikulu m’moyo uno ndi chilango chachikulu
m’moyo umene uli nkudza. Kotero siukadapeza wina
aliyense wokuthandiza ku mkwiyo wathu.
76. Ndithudi adatsala pang’ono kukuchititsa mantha
m’dziko ndi cholinga choti akuchotse m’menemo.
Zikadatheka kutero iwo sakadakhala pambuyo pako, koma
kwa kanthawi kochepa. 77. Umenewu ndiwo mwambo

wa Atumwi amene tidatumiza iwe usanadze ndipo iwe
siudzapeza kusintha kulikonse m'mwambo wathu.
78. Chita mapemphero kuyambira nthawi yopendekera
dzuwa kufikira usiku ndipo werenga Korani m'mapemphero
a m'mbandakucha. Ndithudi kuwerenga Korani nthawi
ya m'mbandakucha kumachitilidwa umboni. 79. Ndipo
m'kati mwa usiku, pemphera ndi kuwerenga Korani ndi
mapemphero oonjezera kwa iwe. Mwina Ambuye wako
angadzakuike pamalo wotamandika.
80. Nena, "Ambuye ndilowetseni kulowa kwa bwino ndipo
nditulutseni mwaubwino. Ndipo ndipatseni kuchokera
kwa Inu mphamvu yondithandiza." 81. Nena, "Choonadi
chadza ndipo bodza latha. Ndithudi bodza liyenera kutha."
82. Ndipo titumiza kuchokera m'Korani mankhwala
ochiza ndiponso chisoni kwa onse okhulupirira, ndipo
imaonjezera kwa anthu osakhulupirira chionongeko.
83. Ndipo tikam'patsa munthu zokoma zathu, iye
amatembenuka ndi kuchita mwano ndipo amakhala kutali
ndi njira yoyenera. Ndipo zikam'peza zoipa amakhala
wotaya mtima kwambiri. 84. Nena, "Munthu aliyense
amachita molingana ndi chikhalidwe chake koma Ambuye
wanu amadziwa yemwe watsogozedwa bwino panjira
yachilungamo."
85. Iwo akukufunsa za Mzimu. Ndipo nena, "Ambuye wanga
ndiye amene adziwa za iwo. Ndipo inu simudapatsidwe
nzeru koma pang'ono pokha."
86. Ndithudi Ife tikadafuna, tikadakulanda chimene
tavumbulutsa kwa iwe ndipo iwe siukadapeza wina aliyense
wokuteteza kwa Ife m'malo mwako. 87. Kupatula chifundo
chochokera kwa Ambuye wako, ndithudi ubwino wake pa

iwe ndi waukulu zedi. 88. Nena, “Ngati anthu ndi majini
akadagwirizana kubweretsa chofanana ndi Korani ino,
iwo sakadabweretsa chofanana nayo ngakhale kuti iwo
akadathandizana.”

89. Ndithudi talongosola kwa anthu mu Korani ino
chitsanzo chilichonse. Komabe anthu ambiri akana
choonadi ndi kukhala osakhulupirira. 90. Iwo amati, “Ife
sitidzakukhulupirira iwe mpaka pamene utatitumphutsira
kasupe kuchokera pansi.” 91. “Kapena utakhala ndi munda
wa tende ndi mphesa ndipo m’kati mwake utumphutse
mitsinje yaikulu.” 92. “Kapena ugwetse mtambo pa ife monga
momwe udatilonjezera kapena utibweretsere Mulungu
pamodzi ndi angelo pamaso pathu.” 93. “Kapena ukhale
ndi nyumba yokongoletsedwa bwino kwambiri kapena
ukwere kumwamba. Komabe ife sitidzakukhulupirira
kukwera kwako mpaka pamene utatitsitsira ife Buku
kuti tiziwerenga.” Nena, “Alemekezeke Ambuye wanga!
Ndithudi ine sindine aliyense koma munthu amene
watumizidwa ngati Mtumwi.”

94. Ndipo palibe chimene chidawaletsa anthu kukhala
okhulupirira pamene malangizo adadza kwa iwo koma
mwano chifukwa iwo amati, “Kodi Mulungu watumiza
munthu kukhala Mtumwi?” 95. Nena, “Ngati angelo
akadakhala pa dziko lapansi, namayenda mwamtendere,
ndithudi, Ife tikadatumiza kwa iwo mngelo kuchoka
kumwamba ngati Mtumwi.” 96. Nena, “Mulungu ndi
wokwana kukhala mboni pakati pa ine ndi inu. Ndithudi!
Iye ndi wodziwa ndi woona zonse za akapolo ake.”

97. Ndipo aliyense amene Mulungu wamutsogolera ,
atsogozedwa bwino koma iye amene Iye amusocheza

wotere iwe siungamupezere mtetezi wina aliyense kupatula Iye yekha. Ndipo Ife tidzawasonkhanitsa onse pa tsiku la kuuka kwa akufa, akuyenda pa nkhope zawo, akhungu, abububu ndi agonthi, malo awo adzakhala Gahena ndipo pamene malawi ake azikazima tizidzawaonjezera moto. 98. Amenewo ndiwo malipiro awo chifukwa iwo sadakhulupirire mawu athu ndipo adati, "Pamene ife tidzasanduka mafupa ndi kufufutika, kodi tidzaukitsidwa kukhala chilengedwe chatsopano?"

99. Kodi iwo saona kuti Mulungu amene adalenga kumwamba ndi dziko lapansi ali ndi mphamvu yolenga zofanana ndi iwo? Ndipo Iye adawaikira iwo nthawi yosakayikitsa. Komabe anthu ochimwa amakana choonadi ndikusankha kusakhulupirira. 100. Nena, "Ngati mukadakhala ndi nkhokwe za chifundo cha Ambuye wanga, ndithudi, inu mukanazibisa poopa kuti zingathe." Ndithudi munthu ndi waumbombo.

101. Ndithudi Ife tidamupatsa Mose zizindikiro zisanu ndi zinayi zooneka. Afunse ana a Israyeli pamene iye adadza kwa iwo ndipo Farawo adati kwa iye, "Iwe Mose, ndithudi, ine ndili kukuganizira kuti ndiwe wolodzedwa." 102. Iye adati, "Ndithudi iwe uli kudziwa bwinobwino kuti zizindikiro izi sizinatumizidwe ndi wina koma Ambuye wakumwamba ndi dziko lapansi ngati umboni wooneka ndi maso. Ndipo, ndithudi, ine ndiganiza kuti iwe, Farawo, ndiwe woonongeka." 103. Farawo anafunitsitsa kuti awapirikitse m'dziko. Koma Ife tidamumiza pamodzi ndi onse amene adali naye. 104. Ndipo pambuyo pake Ife tidati kwa ana a Israyeli, "Khalani m'dziko ndipo pamene lonjezo

lomaliza lidzadza, Ife tidzakusonkhanitsani kukhala malo
amodzi.”
105. Ife tavumbulutsa Buku la Korani m’choonadi ndipo ndi
m’choonadi latsika. Ndipo Ife takutumiza iwe osati wina
kuti ukalalikire nkhani za bwino ndi kupereka chenjezo.
106. Ndi Buku la Korani limene tagawa m’zigawo kuti iwe
uwerenge kwa anthu mwakanthawi. Ife talivumbulutsa
pang’onopang’ono.
107. Nena, “Zili kwa inu kulikhulupirira kapena
kusalikhulupirira. Ndithudi! Iwo amene adapatsidwa nzeru
ilo lisadadze, likamawerengedwa kwa iwo, amagwetsa
mphumi zawo pansi.” 108. Ndipo iwo amati, “Ulemerero
ndi wa Ambuye wathu! Ndithudi lonjezo la Ambuye wathu
likwaniritsidwe.” 109. Ndipo iwo amagwa pansi pa zipumi
zawo, ali kulira ndipo limawaonjezera kudzichepetsa.
110. Nena, “Muitaneni Mulungu kapena Mwini chifundo
chosatha, m’dzina lililonse limene mungamuitanire,
chifukwa Iye ali ndi mayina abwino. Ndipo musanene
mapemphero anu mokweza kapena motsitsa koma
sankhani mawu a pakati ndi pakati.” 111. Nena,
“Kuyamikidwa konse ndi kwa Mulungu, amene sanabale
mwana wamwamuna ndipo alibe mnzake womuthandiza
mu Ufumu wake, ndipo Iye siwopanda mphamvu kuti
angakhale ndi womuthandiza. Motero mulemekezeni Iye
ndi ulemu woyenera Iye yekha.”

# Al-Kahf

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Kuyamikidwa konse kukhale kwa Mulungu amene
wavumbulutsa kwa kapolo wake Buku ndipo sanaike mu
ilo zokayikitsa zina zili zonse. 2. Lolungama kuti lichenjeze
za chilango chowawa chochokera kwa Iye ndi kuwauza
anthu okhulupirira amene amachita ntchito zabwino kuti
adzalandira mphotho yabwino. 3. M'menemo adzakhalamo
mpaka kalekale. 4. Ndi kuchenjeza iwo amene amanena
kuti, "Mulungu wabereka mwana wamwamuna." 5. Pa izi iwo
sadziwa china chilichonse, ngakhale makolo awo. Loopsa
ndi liwu lalikulu limene likutuluka m'kamwa mwawo. Iwo
sanena china koma bodza.
6. Mwina iwe ukhoza kudzipha ndi chisoni chifukwa
chakuti iwo sakhulupirira chivumbulutsochi. 7. Ndithudi!
Ife tazipanga zimene zili m'dziko lapansi kukhala
zokongola ndi cholinga chakuti tiwayese kuti ndani mwa
iwo ali wochita zabwino. 8. Ndithudi! Ife tidzapanga zonse
zimene zili pa dziko kukhala nthaka youma.
9. Kodi iwe ukuganiza kuti anthu a ku phanga ndi
malembo a pa gome ndi zozizwitsa pakati pa zizindikiro
zathu? 10. Pamene anyamata adathawa ndipo adalowa ndi
cholinga chopeza malo kuphanga ndipo adati, "Ambuye
wathu! Tionetseni chisoni chochokera kwa Inu ndipo
tikonzereni zinthu zathu munjira zoyenera." 11. Motero

Ife tidawatseka makutu awo pamene anali kuphanga zaka
zingapo. 12. Ndipo Ife tidawadzutsa kuti tidziwe ndani mwa
magulu awiriwa amene adasunga bwino nthawi imene iwo
adakhala kuphanga.
13. Ife tili kukuuza nkhani zawo zonse mwachoonadi.
Ndithudi! Iwo anali anyamata amene adakhulupirira
mwa Ambuye wawo, ndipo Ife tidawaonjezera malangizo.
14. Ndipo Ife tidalimbitsa mitima yawo, pamene adaima ndi
kunena kuti, "Ambuye wathu ndiye Ambuye wa kumwamba
ndi dziko lapansi. Ife sitidzapembedza mulungu wina
kupatula Iye yekha. Ngati tikatero ndiye kuti tayankhula
bodza lopyola muyeso." 15. Awa anthu athu amatumikira
milungu ina yoonjezera pa Iye. Kodi ndi chifukwa chiyani
iwo sawabweretsera umboni woonekera weniweni?
Kodi wochimwa kwambiri ndani kuposa munthu amene
amapeka bodza lokhudza Mulungu?
16. Pamene inu muwapewa iwo pamodzi ndi zimene iwo
akupembedza osati Mulungu, thawirani kuphanga kuti
mukapeze mpumulo. Ambuye wanu adzakutambasulirani
chisoni chake ndi kukukonzerani njira yoti zinthu
zikupepukireni.
17. Mwina iwe udaona dzuwa pamene linali kutuluka
kupita ku mbali ya manja kwa phanga lawo ndipo pamene
linali kulowa lilikudutsa ku mbali ya manzere, iwo adagona
m'kati mwake. Chimenecho ndi chimodzi cha zizindikiro
za Mulungu. Yense amene Mulungu amutsogolera ndi
wotsogozedwa bwino koma iye amene Iye amusocheza,
iwe siungam'pezere bwenzi woti amutsogolere.
18. Ndipo inu mukadaganiza kuti iwo adali maso pamene
iwo adali mtulo. Ndipo Ife tinali kuwatembenuza kuchoka

ku mbali ya manja kupita ku mbali ya manzere ndipo galu
wawo adali chigonere ndi miyendo yake iwiri ya m'tsogolo
ili yotambasula pa khomo la phanga. Iwe ukadaona iwo
ukadachita mantha ndipo ukadathawa. Ndithudi iwe
ukadadzadzidwa ndi mantha chifukwa cha iwo.
19. Chomwecho Ife tidawadzutsa kuti afunsane wina ndi
mnzake. Wina wa iwo adafunsa nati, "Kodi inu mwakhala
nthawi yotani? Iwo adayankha kuti: 'Ife takhala tsiku
limodzi kapena theka la tsiku.' Iwo adati: "Ambuye wanu
ndiye amene adziwa bwino za nthawi imene mwakhala
kuno. Mtumizeni mmodzi wa inu ku mzinda ndi
ndalama zanu za siliva kuti akagule chakudya chabwino
kuti akubweretsereni. Koma akasamale ndipo asakauze
aliyense za inu." 20. "Chifukwa ngati iwo adzadziwa za
inu, adzakuponyani miyala kapena adzakubwezerani ku
chipembedzo chawo. Ndipo zitatero inu simudzapambana
ayi."
21. Motero Ife tidawadziwitsa anthu za iwo kuti iwo akhoza
kudziwa kuti pangano la Mulungu ndi loona, ndipo kuti
ola la chionongeko, ndithudi, lidzadza popanda chikayiko.
Nthawi imene amakangana pa nkhani zawo za kuphanga
iwo adati; 'Amangireni nyumba pakhomo la phanga lawo.
Ambuye wawo yekha ndiye amene adziwa za iwo.' Ndipo
iwo amene adapambana pa zochita zawo anati: "Ndithudi
Ife tidzamanga malo opembedzerapo pamalopo."
22. Ena a iwo adati, Adali atatu ndipo galu wawo adali
wachinayi, pamene ena akuti adali asanu ndipo galu wawo
adali wachisanu ndi chimodzi. Moganizira zinthu zobisika,
ena akuti adalipo asanu ndi awiri ndipo galu wawo adali
wachisanu ndi chitatu. Nena, "Ambuye wanga ndi wodziwa

kwambiri chiwerengero chawo, palibe amene akuwadziwa
kupatula ochepa okha." Usakangane nawo za iwo kupatula
mkangano womveka. Ndipo usamufunse wina aliyense
wa anthu zokhudza anthu a kuphanga. 23. Ndipo usanene
za china chilichonse kuti, "Ine ndidzachita ichi mawa."
24. Opanda kuonjezera mawu oti, "Ngati Mulungu afuna."
Ndipo kumbukira Ambuye wako ngati uiwala ndipo unene
kuti, "Ngati ndikotheka Mulungu anditsogolere ine ndi
kundibweretsa kufupi ndi choonadi m'malo mwa ichi."

25. Iwo adakhala m'phanga lawo zaka mazana atatu ndi
kuonjeza mphambu zisanu ndi zinayi. 26. Nena, "Mulungu
amadziwa kwambiri mmene adakhalira. Kudziwa zinsinsi
zonse za kumwamba ndi za dziko lapansi ndi kwake. Oh!
Iye amapenyetsetsa ndipo amamvetsetsa. Iwo alibe wina
woti awasamale oposa Mulungu. Ndipo Iye samuphatikiza
wina aliyense mu ulamuliro wake."

27. Werenga zimene zavumbulitsidwa kwa iwe m'Buku la
Ambuye wako. Palibe munthu amene angasinthe mawu
ake. Iwe siudzapeza kothawira kupatula kwa Iye. 28. Pirira
pamodzi ndi iwo amene akupembedza Ambuye wawo
m'mawa ndi madzulo kufuna chisangalalo chake. Maso
ako asayang'ane kutali kuwasiya iwo ndi cholinga chakuti
upeze zinthu zabwino m'moyo uno ndipo usamumvere iye
amene mtima wake tauiwalitsa kuti asamatikumbukire;
ndipo watsatira zofuna za mtima wake, ndipo ntchito zake
zonse ndi zoonongeka.

29. Nena, "Choonadi chimachokera kwa Ambuye wanu.
Amene afuna akhulupirire ndipo amene safuna akane.
Ndithudi anthu oipa tawakonzera moto umene mphanda
zake zidzawazungulira." Pamene iwo adzapempha madzi

akumwa adzapatsidwa madzi otentha ngati mkuwa
wosungunuka amene adzaotcha nkhope zawo. Kuipa kwa
chakumwa ndi kuipa kwa malo okhala ndi kumeneku.
30. Kwa iwo amene akhulupirira nachita zabwino,
ndithudi, Ife sitidzaononga mphotho ya anthu ochita
zabwino. 31. Iwo adzakhala m'minda yamuyaya ndipo
mitsinje izidzayenda pansi pawo. Iwo adzavekedwa
zibangiri za golide ndipo adzavala nsalu za sirika wobiriwira,
wopepuka ndi wochindikala ndipo adzatsamira pa masofa
ndipo malipiro abwino ndi malo abwino ofikira.
32. Auze za fanizo la anthu awiri. Mmodzi wa iwo adali ndi
minda iwiri ya mphesa imene tidazunguliza m'mbali mwake
ndi mitengo ya tende ndipo tidaika pakati pake mbewu
zina. 33. Munda uliwonse umapereka zipatso zake, ndipo
siupunguza chilichonse ndipo Ife tidatumphutsa mitsinje
m'kati mwa mindayo. 34. Ndipo Iye adali ndi zipatso zambiri
ndipo adanena kwa mnzake pamene anali kutsutsana naye
nati, "Ine ndili ndi chuma chambiri kuposa iwe ndiponso
ndili ndi anthu a ntchito amphamvu kwambiri." 35. Ndipo
iye adalowa m'munda mwake modzitukumula yekha
nati, "Ine sindiganiza kuti izi zidzatha ayi." 36. "Ndipo
ine sindikhulupirira kuti ola la chionongeko lidzadza.
Ndipo ngakhale nditabwezedwa kwa Ambuye wanga, ine
ndikapeza malo abwino oposa awa."
37. Mnzake uja adati kwa iye, "Kodi iwe wam'kana Iye
amene adakulenga iwe kuchokera ku dothi ndi kuchokera
ku dontho la umuna ndipo adakuumba kukhala munthu?"
38. Akakhala ine, Mulungu ndiye Ambuye wanga. Ine
sindidzamufanizira Iye ndi china chilichonse. 39. Bwanji
pamene iwe umalowa m'munda mwako, siudanene kuti,

“Izi ndi zimene Mulungu wafuna ndipo kulibe mphamvu
kwina kulikonse kupatula kwa Mulungu? Ngakhale iwe
ukundiona ine kuti ndine wochepekedwa kwambiri
m’chuma ndi ana.” 40. “Mwina Ambuye wanga akhoza
kundipatsa munda wabwino oposa wako ndi kutumiza
ziphaliwali kuchokera kumwamba ndi kusandutsa nthaka
kukhala yosabereka.” 41. “Kapena kuzamitsa madzi ake kuti
iwe usawapeze.”

42. Ndipo zipatso zake zidaonongeka. Ndipo iye
adayamba kufikisa zikhato zake mwachisoni chifukwa
cha zonse zimene adaononga pa mindayi chifukwa
zonse zidaonongeka. Ndipo iye adati: “Kalanga ine!
Ndikanadziwa, sindikanaphatikiza milungu ina ndi
Ambuye wanga!” 43. Ndipo iye adalibe gulu lomuthandiza
polimbana ndi Mulungu ndiponso adalibe mphamvu zoti
adzitetezere kapena kudzipulumutsira. 44. Kumeneko
chitetezo chidzakhala chochokera kwa Mulungu, Mwini
choonadi. Iye ndiye ali ndi malipiro ndiponso mapeto
abwino.

45. Uwapatse chitsanzo cha moyo wa padziko lapansi.
Moyowu uli ngati madzi amene timatsitsa kumwamba
ndi mbeu za padziko la pansi zimene zimasakanizana
ndi iwo ndipo zimakhala zanthete ndi zobiliwira. Koma
pambuyo pake zimauma ndi kufumbutuka ndipo mphepo
imazimwaza. Ndipo Mulungu ali ndi mphamvu pa
chilichonse. 46. Chuma ndi ana ndi zinthu zokongola za
umoyo wadziko lapansi. Koma ntchito zabwino zokhalitsa
ndi zomwe zili ndi malipiro abwino kwa Ambuye wako ndi
chiyembekezo chabwino.

47. Ndi tsiku limene tidzagudubuza mapiri ndipo

mudzaona nthaka ili kukhala poyera popanda chilichonse
ndipo Ife tidzasonkhanitsa anthu onse. Palibe aliyense
amene tidzamusiye mwa iwo. 48. Ndipo iwo adzaonetsedwa
kwa Ambuye wako ataimikidwa m'mizere ndipo tidzanena
kuti, "Ndithudi inu mwabwera kwa Ife monga momwe
tidakulengerani poyamba. Koma inu munali kuganiza kuti
lonjezo lathu silidzakwaniritsidwa ayi."
49. Ndipo Buku lidzaikidwa m'manja mwa aliyense ndipo
iwe udzaona anthu ochita zoipa ali ndi mantha poona zonse
zimene zidalembedwa mu Bukulo. Iwo adzati, "Tsoka
kwa ife! Kodi Buku ili ndi lotani limene silisiya kanthu
kakang'ono kapena kakakulu ndipo zonse lidasunga?"
Ndipo iwo adzapeza ntchito zawo zonse zitalembedwa
momwemo ndipo Ambuye wako sadzapondereza wina
aliyense.
50. Pamene Ife tidawauza angelo kuti, "Mugwadireni
Adamu." Motero onse anamugwadira Iye kupatula Satana
amene adali mmodzi wa ziwanda ndipo adanyoza lamulo
la Ambuye wake. Kodi mudzasankha iyeyo pamodzi ndi
ana ake kukhala okutetezani ndi kukuthandizani m'malo
mwa Ine, pamene iwo ndi adani? Kodi ndi choipa chotani
chimene anthu ochita zoipa asankha?
51. Ine sindidawaonetse kalengedwe ka kumwamba ndi
dziko lapansi kapena kalengedwe kawo komwe ndiponso
Ine sindidawasankhe, osocheretsa anthu, kukhala
ondithandiza anga.
52. Ndi tsiku limene Iye adzati kwa iwo, "Itanani onse
amene mumandifanizira aja, amene munkadzinamiza aja."
Ndipo iwo adzalira kwa iwo koma sadzawayankha ndipo Ife
tidzabzala chidani pakati pawo. 53. Ndipo anthu ochimwa

adzaona moto wa ku Gahena ndipo adzatsimikiza kuti iwo
aulowa. Ndipo iwo sadzapeza njira yothawirako.
54. Ndithudi Ife tawakhazikitsira anthu chitsanzo
chilichonse mu Korani ino. Koma munthu ndi wotsutsa
muzinthu zambiri. 55. Palibe chimene chimawaletsa anthu
kukhulupirira ndi kupempha chikhululukiro kwa Ambuye
wawo pamene chilangizo chidza kwa iwo kupatula kuti ali
kudikira njira za anthu a zaka zakale kuti ziwapeze iwo
kapena kuti akumane ndi mazunzo maso ndi maso.
56. Ndipo Ife sitimangotumiza Atumwi kupatula kuti
akalalikire nkhani yabwino ndi kupereka chenjezo. Koma
anthu osakhulupirira amatsutsa mwabodza kuti agonjetse
choonadi ndi bodza lawo. Ndipo iwo amasandutsa mawu
anga ndi zonse zomwe achenjezedwa ngati nthabwala
kapena choseketsa. 57. Kodi wolakwa kwambiri ndani kuposa
munthu amene akakumbutsidwa mavesi a Ambuye wake
iye amawakana ndi kuiwala zimene manja ake atsogoza?
Ife taika zophimba mitima yawo kuti asazindikire ndipo
tatseka m'makutu mwawo. Ndipo ngati iwe utawaitana
iwo kuti atsatire njira yoyenera, iwo sadzatsogozedwa.
58. Ndipo Ambuye wako ndi wokhululukira kwambiri
ndi Mwini chisoni. Iye akadafuna kuwalanga chifukwa cha
machimo amene achita, ndithudi, Iye akadawafulumizitsira
chilango chawo. Koma iwo ali ndi nthawi yawo ndipo
sadzapeza kothawirako. 59. Ndi Mizinda, imene
tidaiononga pamene eni ake adachita zoipa tidaika nthawi
yachionongeko chawo.
60. Ndipo pamenepo Mose adamuuza mnyamata wake
kuti, "Ine ndidzapitirirabe kuyenda mpaka pamene
ndidzafika pamalo pamene nyanja ziwiri zikumana kapena

ndidzapitirira kuyenda zaka ndi zaka.” 61. Koma pamene
iwo adafika pamalo pamene nyanja ziwiri zidakumana,
iwo adaiwala nsomba yawo ndipo iyo idatenga njira yake
yodutsa kupita m’madzi. 62. Ndipo iwo atapitiriza ulendo
wawo, Mose adati kwa mnyamata wake, “Bweretsa
chakudya chathu. Ndithudi tapeza, mu ulendo wathu,
zotopetsa.”

63. Iye adati, “Kodi iwe siudaone pathanthwe pamene
tidapuma paja, kuti ine ndidaiwala nsomba ndipo palibe
china chimene chidandiiwalitsa kuti ndiikumbukire koma
Satana yemwe adandiiwalitsa. Ndipo iyo idalowa m’madzi
mozizwitsa.” 64. Mose adati, “Pamenepo ndi pamene
timafuna.” Iwo adabwerera kulondola kumene adachokera.
65. Ndipo iwo adam’peza mmodzi wa akapolo wathu amene
tidamupatsa chifundo chochokera kwa Ife ndiponso
tidamuphunzitsa nzeru zochokera kwa Ife.

66. Mose adati kwa iye, “Kodi ndingakutsateni kuti
mwina mundiphunzitse zabwino zina za zimene
mudaphunzitsidwa?” 67. Iye adati, “Ndithudi! Iwe
siudzatha kupirira ndi ine.” 68. Kodi iwe ungapirire bwanji
pa zinthu zimene suli kuzidziwa? 69. Mose adati, “Ngati
Mulungu afuna, udzandipeza ine ndili wopirira ndipo
ine sindidzakunyoza iwe ayi.” 70. Iye adati, “Ngati iwe
unganditsatire, usandifunse china chilichonse chimene
ungawone mpaka pamene ine nditakuuza za chinthucho.”

71. Motero iwo adanyamuka ndipo pamene iwo adakwera
m’chombo, mnzake wa Mose adaboola chombocho. Mose
adati, “Kodi waboola dzenje pa chombochi ndi cholinga
chofuna kumiza eni ake? Ndithudi ichi ndi chinthu
choipa kwambiri chimene wachita!” 72. Iye adati, “Kodi

sindidakuuze kuti iwe siudzatha kupirira ndi ine?” 73. Mose
adati, “Musandidzudzule chifukwa cha zimene ndaiwala
ndipo musandisenzetse katundu wolemera chifukwa cha
zochita zanga.” 74. Ndipo onse adapitirizabe ulendo wawo
mpaka pamene adakumana ndi mnyamata wina amene iye
adamupha. Ndipo Mose adati, “Kodi iwe wapha munthu
wosalakwa amene sadaphepo wina aliyense? Ndithudi iwe
wachita chinthu choipa kwambiri.”

75. Iye adati, “Kodi ine sindidakuuze kuti iwe siudzatha
kupirira ndi ine?” 76. Mose adati, “Ngati ine ndikufunsanso
chinthu china pambuyo pa izi, usayende nanenso chifukwa
ukhala utachipeza chifukwa kuchokera mwa ine.” 77. Ndipo
onse adapitirira kuyenda mpaka pamene adapeza anthu a
mu mzinda wina wake ndipo iwo adawafunsa anthu aja kuti
awapatseko chakudya koma iwo adakana kuwalandira ngati
alendo awo. Iwo adapeza mu mzindawo chipupa chikufuna
kugwa ndipo Iye adachimanganso. Mose adati, “Iwe
ukadafuna, ndithudi, ukadawauza kuti akulipire chifukwa
cha ntchito imene wagwira.” 78. Iye adati, “Uku ndiye
kusiyana kwa pakati pa iwe ndi ine. Ndikuuza tanthauzo la
zinthu zimene iwe umakanika kupirira nazo.”

79. Chikakhala chombo chija eni ake adali anthu
osauka amene amagwira ntchito pa nyanja. Ndipo ine
ndinafuna kuti ndichiononge chifukwa kutsogolo kwawo
kudali mfumu yomwe imalanda chombo chilichonse
mwamphamvu.

80. Akakhala mnyamata uja, makolo ake onse adali
okhulupirira mu choonadi ndipo timaopa kuti mwina iye
akhoza kuwatembenuza ndi kuyamba kuchita zoipa ndi
kusiya kukhulupirira. 81. Ndipo tidafuna kuti Ambuye

wawo awapatse m’malo mwake, mwana wina wabwino ndi
woyera mtima kuposa iye.
82. Chikakhala chipupa chija, eni ake adali ana awiri a
masiye amene amakhala mu mzinda uja ndipo pansi pa
chipupacho padali chuma chawo. Ndipo bambo wawo
adali munthu wabwino motero Ambuye wako adafuna kuti
anawo akule kuti adzatulutse okha chuma chawo ngati
chifundo chochokera kwa Ambuye wako. Ine sindidachite
zimenezi mwachifuniro changa ayi. Limeneli ndilo
tanthauzo lake la zinthu zimene umalephera kupirira nazo.
83. Ndipo iwo akukufunsa za Dhul-Qarnain. Nena,
“Ine ndikufotokozerani za mbiri ya iye.” 84. Ndithudi
Ife tidamukhazika iye padziko ndipo tidamupatsa njira
yopezera chilichonse.
85. Ndipo iye adatsatira njira. 86. Mpaka pamene adafika
polowera dzuwa ndipo adalipeza dzuwalo lili kulowa
m’dziwe la matope akuda. Pafupi pomwepo iye adapeza
anthu ena. Ife tidati, “Iwe Dhul-Qarnain! Iwe uli ndi ufulu
wowalanga kapena wowachitira chisoni.” 87. Iye adati,
“Akakhala iye amene achita zoipa, tidzamulanga ndipo iye
adzabwezedwa kwa Ambuye wake yemwe adzamulanga
ndi chilango choipa kwambiri.” 88. Koma iye amene
wakhulupirira ndikumachita ntchito zabwino, adzakhala
ndi mphotho yabwino ndipo tidzamuyankhula mawu
abwino.
89. Ndipo iye adatsatira njira ina. 90. Mpaka pamene
adafika kotulukira dzuwa kumene adalipeza dzuwa lili
kutuluka pa anthu amene Ife sitidawaikire chotchinga ku
dzuwa. 91. Kotero Ife tidadziwa zonse zokhudza iye.
92. Ndipo iye adatsatiranso njira ina. 93. Mpaka pamene iye

adafika pakati pa mapiri awiri adapeza pambali pake anthu
amene sanali kuzindikira chilichonse. 94. Iwo adati, "Iwe
Dhul-Qarnain! Ndithudi Ya-juj ndi Majuj ali kuchita zoipa
m'dziko lino. Kodi tikupatse malipiro kuti utimangire linga
lotiteteza nalo pakati pa iwo ndi ife?"
95. Iye adati, "Mphamvu zomangira linga zimene Ambuye
wanga wandipatsa ndi zabwino. Choncho ndithandizeni
ndi anthu amphamvu ogwira ntchito kuti ndimange linga
pakati pa inu ndi iwo." 96. Ndipatseni zidutswa zachitsulo;
mpaka pamene iye adadzadza gawo limene linali pakati pa
mapiriwa. Iye adati, "Uzirani ndi livumbo lanu." Pamene
adazifiwiritsa zidutswazo ngati moto, iye adati, "Ndipatseni
mtovu kuti ndiuthire pa zidutswazo." 97. Anthu a Ya-juj ndi
Majuj sadathe kuchilumpha ndipo sadathe kuchiboola.
98. Iye adati, "Ichi ndi chifundo chochokera kwa Ambuye
wanga. Koma pamene lonjezo la Ambuye wanga lidzadza,
Iye adzalionongа. Ndipo lonjezo la Ambuye wanga ndi
loona.
99. Ndipo pa tsikulo tidzawasiya ena mwa iwo
akusakanikirana ndi ena. Lipenga lidzaimbidwa ndipo
tidzawasonkhanitsa onse pamodzi. 100. Pa tsiku limeneli
tidzaonetsa Gahena kwa anthu osakhulupirira, kuti
adzalione lonse moonekera kwambiri. 101. Amene maso
awo adali otsekeka kuchikumbutso changa, satha kumva.
102. Kodi anthu osakhulupirira akuganiza kuti akhoza
kuwapanga akapolo anga kukhala atetezi awo m'malo mwa
Ine? Ndithudi Ife takonza Gahena kukhala malo ofikira
anthu onse osakhulupirira.
103. Nena, "Kodi tikuuzeni anthu amene ali olephera
mu ntchito zawo?" 104. Iwowo ndi amene ntchito zawo

zaonongeka m'moyo uno pamene iwo anali kuganiza kuti
ali kulandira zabwino chifukwa cha ntchito zawo. 105.
Iwo ndi amene sadakhulupirire mawu a Ambuye wawo
ndi zokumana ndi Iye. Motero ntchito zawo zaonongeka
ndipo patsiku lachiweruzo Ife sitidzawakhazikira muyeso.
106. Gahena idzakhala mphotho yawo chifukwa iwo adalibe
chikhulupiriro ndipo achitira chipongwe Atumwi ndiponso
mawu anga.

107. Ndithudi! Iwo amene akhulupirira ndi kuchita
ntchito zabwino, minda ya ku Paradiso idzakhala malo
awo ofikira. 108. Adzakhala komweko nthawi zonse ndipo
sadzafuna kusintha malo.

109. Nena, "Ngati Nyanja ikadakhala inki yolembera mawu Ambuye wanga, ndithudi, nyanjayo ikadaphwa koma osati Mawu a Ambuye wanga ngakhale tikadabweretsa nyanja yofanana ndi imeneyo moonjezera."

110. Nena, "Ine ndine munthu monga inu nomwe, koma zavumbulutsidwa kwa ine kuti Mulungu wanu ndi mmodzi. Kotero aliyense amene afuna kudzakumana ndi Ambuye wake ayenera kuchita zimene zili zabwino ndipo popembedza Ambuye wake, osaphatikizamo wina wake."

# Marium

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. *Kaf ha ya ain suad.*

2. Ichi ndi chikumbutso cha chifuniro cha Ambuye wako
kwa kapolo wake Zakariya. 3. Pamene Iye adamupempha
Ambuye wake motsitsa mawu. 4. Iye adati, "Oh Ambuye
wanga! Mafupa anga ndi ofoka ndipo mutu wanga uli
ndi imvi chifukwa cha ukalamba. Komabe, Ambuye, ine
sindidapemphe kwa Inu mopanda phindu." 5. "Ndithudi ine
ndili ndi mantha ndi abale anga za amene adzalowe m'malo
mwanga ndiponso mkazi wanga ndi chumba. Ndipatseni
mwana wamwamuna." 6. "Amene adzalowe m'malo mwanga
ndi m'malo mwa ana a Yakobo, ndipo mpangeni, Ambuye
wanga, kukhala mmodzi wa wokondedwa wanu."
7. "Ee iwe Zakariya! Ife tili kukuuza nkhani yabwino
yakuti iwe udzapatsidwa mwana wamwamuna ndipo
adzatchedwa Yohane, dzina limene silidapatsidwe kwa
aliyense kumbuyoku." 8. Zakariya adati, "Ambuye! Kodi
ine ndingakhale ndi mwana wamwamuna bwanji, pamene
mkazi wanga ndi chumba ndipo ine ndine wokalamba?"
9. Iye adati, "Chimenechi, wanena Ambuye wako!
Idzakhala ntchito yopepuka kwa Ine chifukwa Ine
ndidakupanga kukhala munthu pamene iwe siunali chinthu
china chilichonse chodziwika." 10. Zakariya adati, "Ambuye,
ndipatseni chizindikiro chokhudza zimene zidzachitike."

Iye adati, “Chizindikiro chako ndi chakuti siudzalankhula
ndi anthu usiku utatu ngakhale ulibe chilema.” 11. Pamene
Zakariya adadza kwa anthu ake kuchokera m’kachisi,
adawauza anthuwo kuti, “Lemekezani Ambuye wanu
m’mawa ndi madzulo.”
12. “Oh Yohane! Samala mawu a Mulungu kwambiri.” Ife
tidamupatsa luntha pamene adali mwana. 13. Ndiponso
tidamupatsa mtima wachifundo ndi woyeretsedwa ndipo
adali munthu opewa zoipa. 14. Ndipo adali kulemekeza
abambo ndi amayi ake. Iye sadali wodzikweza kapena
wonyoza malamulo a Mulungu. 15. Mtendere udali pa iye
pa tsiku limene adabadwa ndi pa tsiku limene adafa ndipo
mtendere ukhale pa iye pamene aukitsidwa kwa akufa.
16. Ndipo kukumbukira nkhani ya Maria m’Buku!
Pamene iye adasiya anthu ake ndi kupita kumalo a payekha
kumbali ya ku m’mawa. 17. Ndipo iye adafunda nsalu kuti
anthu asaone nkhope yake. Ife tidamutumizira iye Mzimu
wathu umene udaoneka ngati munthu. 18. Maria adati,
“Mwini chisoni anditeteze ine kwa iwe! Ngati iwe umaopa
Ambuye, ndisiye ndekha, usandiyandikire ayi.” 19. Mngelo
adati, “Ine ndine Mthenga wa Ambuye wako ndipo ndadza
kudzakupatsa mwana wamwamuna woyera.” 20. Maria
adati, “Kodi ine ndidzabereka mwana bwanji pamene ine
ndine wosakhudzidwa ndi mwamuna ndiponso si ndine
wachiwerewere ayi?” 21. Mngelo adati, “Ndi momwemo”
Ambuye wako wanena kuti, “Zimenezo, kwa Ine, ndi
zopepuka. Tidzamupanga iye kukhala chizindikiro kwa
anthu ndi madalitso ochoka kwa Ife. Limeneli ndilo lamulo
limene lalamulidwa.”
22. Ndipo iye adakhala ndi pakati ndipo adapita kumalo

akutali. 23. Ndipo ululu wa kubereka udamubwerera
pamene adali patsinde pa mtengo wa tende ndipo adalira
nati, “Kalanga ine, bola ndikadangofa zisanachitike izi
chifukwa ndikadakhala woiwalidwa.”

24. Kudabwera mawu kuchokera pansi oti: “Usadandaule
ayi. Ambuye wako wakukonzera ka mtsinje kamene
kalikuyenda ku mapazi ako.” 25. “Ndipo gwedeza mtengo
watendewu, iwo udzagwetsa zipatso za tende zaziwisi ndi
zakupsa.” 26. “Idya ndi umwe, kotero sangalala.” Ndipo
ukakumana ndi munthu wina aliyense muuze kuti, “Ine
ndalumbira kwa Mwini chisoni kusala chakudya ndipo
sindidzayankhula ndi munthu wina aliyense lero.”

27. Ndipo iye adatenga mwana wake nanka naye kwa
anthu ake amene adati kwa iye’ “Iwe Maria! Ndithudi
iwe wabweretsa chinthu cha chilendo.” 28. “Iwe mlongo
wake wa Aroni! Atate wako sanali munthu wochita zoipa
ndiponso Amayi ako sadali a chiwerewere.”

29. Maria adamuloza iye. Koma iwo adati, “Kodi
ife tingayankhule ndi mwana wam’chikuta bwanji?”
30. Mwanayo adati, “Ine ndine kapolo wa Mulungu.
Iye wandipatsa ine Buku labwino ndipo wandisankha
kukhala Mtumwi.” 31. “Madalitso ake ali pa ine kulikonse
kumene ndingapite ndipo wandilamulira kuti ndikhale
wopemphera ndi kupereka chaulere kwa anthu osauka
nthawi yonse ya moyo wanga.” 32. “Iye wandilamula kuti
ndizilemekeza amayi anga ndipo sadandipange kukhala
wamwano ndi woipa.” 33. Ndipo mtendere ukhale kwa ine
patsiku limene ndidabadwa, ndi patsiku limene ndidzafa
ndiponso pa tsiku limene ndidzaukitsidwa kwa akufa.

34. Ameneyo ndiye Yesu, mwana wa Maria. Liwu loonadi

limene iwo ali kukayika. 35. Sizili zoyenera kuti Mulungu
akhale ndi mwana wamwamuna! Iye ayeretsedwe ku
zimenezo. Ngati Iye afuna chinthu, Iye amangonena kuti,
"Chikhale" ndipo chimakhaladi.
36. Ndithudi Mulungu ndi Ambuye wanga ndiponso
Ambuye wanu. Kotero mpembedzeni Iye yekha. Imeneyo
ndiyo njira 37. Koma magulu a Akhirisitu adasemphana
maganizo pakati pawo. Koma pamene tsiku loopsa lidza,
tsoka kwa anthu osakhulupirira. 38. Kodi iwo adzaona ndi
kumva momveka bwanji pa tsiku limene adzaonekera
pa maso pathu! Koma anthu ochita zoipa lero ali mu
chisokonezo choonekeratu.
39. Achenjeze za tsiku limene adzanong'oneza bombono,
pamene malamulo athu adzakwaniritsidwa ndipo pamene
iwo ali nkuiwala ndi kusakhulupirira. 40. Ndithudi Ife
tidzatenga dziko lapansi ndi onse amene amakhala
m'menemo. Ndi kwa Ife kumene onse adzabwezedwa.
41. Ndipo kumbukira nkhani ya Abrahamu imene
ili m'Buku. Iye adali Mtumwi ndi munthu wangwiro.
42. Pamene iye adawauza bambo wake kuti, "Oh Abambo!
Kodi inu mungalambire bwanji chinthu chimene
sichingathe kumva, kuona kapena kukuthandizani pa
chilichonse?" 43. "Oh abambo! Choonadi chavumbulutsidwa
kwa ine chimene sichinakufikireni inu. Kotero nditsatireni
ine kuti ndikutsogolereni ku njira yoyenera." 44. "Oh
abambo! Musamapembedze Satana. Ndithudi Satana
adanyoza Ambuye wachisoni chosatha." 45. "Oh abambo!
Ine ndili kuopa kuti chilango cha Mulungu chidzadza pa
inu ndipo mudzakhala bwenzi la Satana."
46. Abambo ake adati, "Kodi ukudana ndi milungu yanga

iwe Abrahamu? Ukapanda kusiya ndidzakuponya miyala
ndipo unditalikire pa kanthawi kochepa.” 47. Abrahamu
adati, “Mtendere ukhale kwa inu. Ine ndidzapempha
Ambuye wanga kuti akukhululukireni popeza, Mulungu,
kwa ine, ndi wokoma mtima.” 48. “Ine ndikuchokerani
ndi zimene mumapembedza kuonjezera pa Mulungu. Ine
ndidzapempha kwa Ambuye wanga ndipo ndikhulupirira
kuti popembedza Ambuye wanga ndisadzakhale watsoka.

49. Ndipo pamene Abrahamu adasiya anthu ake ndi
mafano amene iwo anali kupembedza kuonjezera pa
Mulungu, tidamupatsa Isake ndi Yakobo. Aliyense wa iwo
tidamupanga kukhala Mtumwi. 50. Ndipo tidawapatsa
onse mituka kuchokera m’chifundo chathu ndipo
tidawapanga iwo kukhala otchulidwa mwaulemu. 51. Ndipo
kumbukira nkhani ya Mose imene ili m’Buku, amene
adali wosankhidwa ndiponso Mtumwi ndi Mneneri. 52. Ife
tidamuitana kuchokera kumbali ya dzanja la manja la phiri
la Sinai ndipo tinamuyandikitsa kukhala pafupi ndi Ife kuti
tiyankhule naye mwamseri. 53. Tidamupatsa, mwachisoni
chathu, m’bale wake Aroni kuti akhale Mtumwi.

54. Ndipo kumbukira nkhani ya Ishimayeli imene ili
m’Buku. Iye adali wosunga pangano ndipo adali Mtumwi
ndi Mneneri. 55. Iye anali kulamula anthu ake kuchita
mapemphero ndi kupereka chothandiza nacho anthu
osauka ndipo adali, kwa Ambuye wake, wokondedwa.
56. Ndipo kumbukira za Idrissa. Iye adali munthu wonena
zoona ndi Mtumwi. 57. Ife tidamukweza kukhala malo a
pamwamba.

58. Awa ndi anthu amene Mulungu adawaonetsera
chisomo chake. Atumwi ochokera ku m’badwo wa Adamu

ndi iwo amene tidawatenga pamodzi m’chombo ndi Nowa. Ana a Abrahamu, a Israyeli ndi iwo amene Ife tawatsogolera ndi kuwasankha. Pamene zivumbulutso za Mwini chisoni chosatha zinali kulakatulidwa kwa iwo, iwo adali kugwa nkhope zawo pansi ndi kumalira.

59. Koma mibadwo ya anthu imene inadza iwo atachoka idanyoza mapemphero ndi kutsatira zilakolako zawo. Ndithudi awa adzakumana ndi mavuto. 60. Kupatula amene alapa machimo ndi kukhulupirira choonadi ndi kumachita ntchito zabwino. Iwo adzalowa ku Paradiso ndipo sadzaponderezedwa m’chilichonse.

61. Iwo adzakhala m’minda ya Edeni mpaka muyaya, imene Mwini chisoni chosatha adalonjeza akapolo ake ngakhale kuti iwo sadaione. Ndithudi lonjezo lake lidzakwaniritsidwa. 62. Kumeneko iwo sadzamva zinthu zopanda pake koma mawu a mtendere okha, ndipo chakudya chidzapatsidwa kwa iwo m’mawa ndi madzulo. 63. Imeneyo ndiyo Paradiso imene tidzawapatsa akapolo athu omwe anali kuopa Mulungu.

64. Ife sititsika kuchoka kumwamba pokhapokha ngati taloledwa ndi Ambuye wako. Iye ndiye mwini wa zinthu zonse zimene zili pamaso pathu, kumbuyo kwathu ndi zonse zimene zili pakati pa zimenezi. Ndipo Ambuye wako saiwala. 65. Ambuye wa kumwamba ndi dziko lapansi ndi zonse zimene zili mmenemo. Kotero m’pembedze Iye yekha ndipo khala wopirira pamapemphero ake. Kodi ukudziwa wina amene ali ndi dzina ngati la Iye?

66. Munthu amati, “Pamene ine nditafa kodi ndidzaukitsidwa ndi kukhalanso ndi moyo?” 67. Kodi munthu sakumbukira kuti tidamulenga iye pamene

poyamba sadali chinthu china chilichonse? 68. Motero pali Ambuye wako; ndithudi Tidzawasonkhanitsa pamodzi ndi a Satana ndipo onse tidzawabweretsa m'mphepete mwa Gahena atagwada.

69. Ndipo mwachoonadi tidzachotsa mugulu lililonse onse amene adanyoza Mulungu kwambiri. 70. Ndithudi Ife tilikuwadziwa kwambiri amene ali oyenera kuotchedwa. 71. Palibe wina wa inu amene sadzapita kumbali ya Moto. Limeneli ndilo lamulo la mphamvu la Ambuye wanu. 72. Ndipo Ife tidzapulumutsa onse amene amaopa ndi kuwasiya ochita zoipa, atagwada, kuti amve ululu wake.

73. Pamene zivumbulutso zathu zilakatulidwa momveka kwa iwo, anthu osakhulupirira amanena kwa anthu okhulupirira kuti, "Kodi ndi gulu liti pa magulu awiriwa limene lili ndi malo abwino okhala ndi anthu apamwamba?" 74. Kodi ndi mibadwo ingati yakale imene tidaononga iwo asanadze, mibadwo imene idali ndi zinthu zabwino ndiponso zokongola?

75. Nena, "Aliyense amene alakwa, Mwini chisoni chosatha adzawaonjezera nthawi, mpaka pamene adzaone zomwe adalonjezedwa. Kaya ndi chilango kapena ola lomaliza, pamenepo ndiye adzadziwa kuti ndani amene ali mwini wa malo oipa ndi gulu lankhondo lofoka."

76. Mulungu amapitiriza kutsogolera iwo amene atsatira njira yoyenera. Ntchito zabwino zimene zili ndi malipiro osatha zili ndi mphotho yabwino pamaso pa Ambuye wako ndiponso zotsatira zake ndi zabwino.

77. Kodi mwamuona munthu amene akana zivumbulutso zathu ndipo amanena kuti, "Ine, ndithudi, ndidzapatsidwa chuma ndi ana?" 78. Kodi iye waziona zinthu zosaoneka

kapena Mwini chisoni chosatha wamupatsa lonjezo
lotere? 79. Osatheka! Ife tidzalemba zimene akunena ndi
kuchipanga chilango chake kukhala chachitali. 80. Zonse
zimene azilankhula iye zidzabwerera kwa Ife ndipo
adzadza pamaso pathu yekha. 81. Anthu osakhulupirira
adadzisankhira milungu ina kuti iwapatse mphamvu ndi
ulemerero. 82. Ayi. Koma milunguyo idzakana kupembedza
kwawo ndipo idzakhala adani awo.

83. Kodi siudaone kuti timatumiza kwa anthu
osakhulupirira a Satana amene amawaonetsa zinthu zoti
achimwe nazo? 84. Kotero musafulumize kuwapemphera
chionongeko, ndithudi, tikuwawerengera masiku awo.
85. Tsiku limene tidzasonkhanitsa anthu olungama m'magulu
kufika pamaso pa Ambuye wachisoni kudzalandira ulemu.
86. Ndipo tidzawakusa anthu oipa kupita ku moto wa ku
Gahena ali ndi ludzu lodetsa nkhawa. 87. Palibe amene
adzakhala ndi mphamvu zodandaula kupatula yekhayo
amene walandira chilolezo cha Mwini chisoni chosatha.

88. Iwo amati, "Mwini chisoni chosatha wabala mwana
wamwamuna." 89. Ndithudi mwanena chinthu choipitsitsa.
90. Pafupifupi kumwamba kumafuna kung'ambika
chifukwa cha mawu amenewa ndipo nthaka imafuna
kugawikana ndi mapiri kugudubuzika ndi kuonongeka.
91. Chifukwa chonena Mwini Chisoni Chosatha ali ndi
mwana wamwamuna. 92. Si zoyenera kwa Mwini chisoni
chosatha kuti akhale ndi mwana. 93. Palibe china chilichonse
chimene chili kumwamba kapena pa dziko lapansi chimene
chimabwera kwa Mwini chisoni chosatha kupatula ngati
kapolo. 94. Iye wasunga chiwerengero cha zolengedwa
zake zonse. 95. Ndipo onse, mmodzimmodzi, adzabwerera

kwa Iye pa tsiku la kuuka kwa akufa. 96. Ndithudi amene akhulupirira ndi kuchita ntchito zabwino, Mwini chisoni chosatha adzawakonda.

97. Motero Ife tapanga iyo kukhala yosavuta ya m'chiyankhulo chako kuti upeleke nkhani yabwino kwa anthu oopa ndi kuchenjeza ndi ilo anthu otsutsa.
98. Kodi ndi mibadwo ingati imene Ife tidaononga kale iwo asanadze? Kodi uli kumuona mmodzi aliyense wa iwo kapena kumva manong'onong'o ochokera kwa iwo?

Sura 20 • Tâ-Hâ

# Ta Ha

M'dzina la Mulungu, Mwini chifundo ndi Mwini chisoni chosatha.

1. *Ta Ha.*

2. Ife sitidavumbulutse Korani ino kwa iwe ndi cholinga
choti uvutike. 3. Koma kuti chikhale chilangizo kwa
anthu oopa Mulungu. 4. Ndi chivumbulutso chochokera
kwa Iye amene adalenga dziko lapansi ndi kumwamba
kwenikweniko. 5. Mwini chisoni chosatha amene adaoneka
ali pamwamba pa Mpando wa Chifumu. 6. Zake ndi zonse
zimene zili kumwamba ndi pa dziko lapansi ndi zonse zimene zimakhala m'menemo ndiponso zimene zili pansi pa nthaka.

7. Ngati iwe utchula mawu mokweza, ndithudi Iye
amadziwa chinsinsi ndiponso chobisika. 8. Mulungu! Kulibe

wina wopembedzedwa mwachoonadi koma Iye yekha. Ake
ndi mayina okongola.
9. Kodi udamva za mbiri ya Mose? 10. Pamene iye adaona
moto adawauza abale ake kuti, “Dikirani! Ndithudi ine
ndaona moto. Mwina ndikubweretserani muuni kuti
ndipeze ulangizi pa motopo.”
11. Pamene iye adafika pafupi ndi moto, adaitanidwa
pomutchula dzina lake kuti, “Oh Mose!” 12. “Ndithudi,
Ine ndine Ambuye wako! Motero chotsa nsapato
zako. Ndithudi iwe uli m’dambo lodalitsika la Tuwa.”
13. “Ndipo Ine ndakusankha iwe. Kotero mvetsera chimene
chikuvumbulutsidwa kwa iwe.” 14. Ndithudi Ine ndine
Mulungu. Palibe wina wopembedzedwa mwachoonadi
koma Ine ndekha motero ndipembedze Ine ndipo pitiriza
mapemphero pondikumbukira Ine.” 15. “Ndithudi ola lili
nkudza ndipo cholinga changa ndi kulibisa kuti mzimu
ulionse udzalipidwe malipiro molingana ndi ntchito zake.”
16. “Ndipo usalole kuti munthu amene sakhulupirira za olali
ndipo yemwe amachita zimene mtima wake umafuna kuti
akusocheretse chifukwa ukhoza kuonongeka.”
17. “Kodi ndi chiyani chimene chili m’dzanja lako la manja
iwe Mose?” 18. Iye adati, “Iyi ndi ndodo yanga, ndi iyoyi ine
ndimayedzamira ndipo ndimagwetsera masamba akudya
nyama zanga. Imeneyi imandithandiza pa ntchito zambiri
kuonjezera pa zimenezi.” 19. Mulungu adati, “Ndodoyo
iponye pansi iwe Mose.” 20. Mose adaiponya pansi, ndipo
taonani! Iyo idasanduka njoka yoyenda mwaliwiro.
21. Mulungu adati, “Igwire ndipo usachite mantha ayi.
Ife tidzaibwezera monga momwe idalili poyamba.”
22. “Tsopano kanikiza dzanja lako m’khwapa mwako. Ilo

lidzasanduka loyera lopanda matenda ngati chizindikiro
china.” 23. “Kuti tikusonyeze zizindikiro zathu zazikulu.”
24. “Pita kwa Farawo! Ndithudi iye wadumpha malire onse.”
25. Mose adati, “Ambuye tsekulani chifuwa changa”
26. “Ndipo pepukitsani ntchito yanga.” 27. “Masulani lilime
langa ku chibwibwi.” 28. “Kuti anthu azindikire zonena
zanga.” 29. “Ndipo ndisankhileni munthu wondithandiza
kuchokera ku banja langa.” 30. “Aroni m’bale wanga.”
31. “Onjezereni mphamvu zanga ndi iye.” 32. “Ndipo muloleni
nayenso kugwira ntchito yanga.” 33. “Kuti tizikulemekezani
kwambiri.” 34. “Ndi kukukumbukirani kwambiri.”
35. “Ndithudi! Inu muli kutiona nthawi zonse.” 36. Mulungu
adati, “Pempho lako lalandiridwa, iwe Mose.”
37. “Ndithudi Ife tidakuonetsa chifundo chathu nthawi
ina.” 38. “Pamene tidawauza Amayi ako mawu athu.”
39. Ponena kuti, “Ika mwana wako m’bokosi ndipo
umuponye mu mtsinje ndipo mtsinje udzamulavula iye pa
mtunda ndipo adzatoledwa ndi mdani wanga ndiponso ndi
mdani wake. Ndipo Ine ndidaonetsa chikondi changa pa
iwe kuti uleredwa moyang’aniridwa ndi Ine.” 40. “Ndipo
pamene mlongo wako adapita kwa iwo ndi kunena kuti,
Kodi ndikusonyezeni Mayi amene akhoza kumusamala
iye? M’menemo ndi mmene tidakubwezera kwa Amayi
ako kuti mtima wawo ukhoza kukhazikika ndipo kuti
asakhumudwe. Ndipo pamene iwe udapha munthu, Ife
tidakupulumutsa ku mavuto ako, ndipo tidakuyesa ndi
mayeso ena. Iwe udakhala pakati pa anthu a ku Midiyani
zaka zambiri ndipo pomaliza, iwe Mose, udabwera kuno
monga momwe zidakonzedwera.”
41. “Ine ndakusankha iwe kuti unditumikire Ine.” 42. “Pita

iwe ndi m'bale wako ndi zizindikiro zanga ndipo musatope
pondikumbukira Ine." 43. "Pitani, nonsenu, kwa Farawo
yemwe wadumpha malire." 44. "Ndipo mukayankhule
naye ndi mawu oleza kuti mwina akhoza kumva chenjezo
kapena kuopa Mulungu."

45. Iwo adati, "Ambuye wathu! Ndithudi! Ife tiopa kuti
abweretsa chilango chake msanga kapena achita zoipa
zambiri kwa ife." 46. Iye adati, "Musaope! Ndithudi!
Ine ndili pamodzi ndi inu. Ine ndimamva zonse ndipo
ndimaona." 47. "Motero pitani nonse kwa iye ndipo mukati,
'Ndithudi ife ndife Atumwi Ambuye wako motero aleke
ana a Israyeli kuti apite ndi ife ndipo usawazunzenso ayi.
Ndithudi ife takubweretsera zizindikiro zochokera kwa
Ambuye wako! Ndipo mtendere udzakhala kwa iye amene
atsatira langizo." 48. "Ndithudi zavumbulutsidwa kwa ife
kuti chilango chake chidzagwa pa iye amene amakana
zizindikiro zake ndipo sazimvera ayi."

49. Farawo adati, "Kodi Mose, Ambuye wanu ndani?"
50. Iye adati, "Ambuye wathu ndiye amene adapereka
maonekedwe osiyanasiyana ku zolengedwa zake ndipo
adazilangiza bwinobwino." 51. Farawo adati, "Nanga
zinali bwanji ndi anthu a masiku akale?" 52. Iye adati,
"Ambuye wanga yekha ndiye amene adziwa zimenezo
ndipo zidalembedwa mu Buku lake. Iye salakwa ndiponso
saiwala."

53. Amene adakupangirani dziko lapansi kukhala ngati
kama ndipo adakhazikitsa njira zoti inu muziyendamo
ndipo watumiza mvula kuchokera kumwamba. Ndipo
ameretsa ndi iyo mitundu yosiyanasiyana ya mbewu.
54. Idyani ndiponso dyetsani ziweto zanu. Ndithudi

muzimenezi muli zizindikiro kwa anthu ozindikira.
55. Kuchokera ku dothi tidakulengani inu ndipo ndi ku
nthaka kumene tidzakubwezerani ndipo kuchoka ku iyo
tidzakuutsani kuti mukhalenso ndi moyo kachiwiri.
56. Ndithudi tidamulangiza Farawo zizindikiro ndi
umboni wathu koma iye adazikana zonse ndipo sadamvere
ayi. 57. Iye adati, "Kodi iwe Mose wadza kudzatichotsa
m'dziko lathu ndi matsenga ako?" 58. "Ndithudi ife tikhoza
kukubweretsera matsenga olingana ndi ako. Motero
sankha tsiku limene ife kapena iwe siudzalephera kusunga
loti tidzakumane iwe ndi ife, pa bwalo pamene tonse
tidzakhala ndi mwai wofanana."
59. Mose adati, "Tsiku lokumana lidzakhale tsiku la
chisangalalo ndipo anthu adzasonkhanitsidwe nthawi
ya ku m'mawa dzuwa litakwera pang'ono." 60. Farawo
adachokapo ndipo adasonkhanitsa a matsenga ake ndipo
adadza nawo kwa Mose. 61. Mose adati kwa iwo, "Tsoka
kwa inu! Musapeke mabodza okhudza Mulungu chifukwa
akhoza kukuonongani ndi chilango. Ndipo, ndithudi,
aliyense amene apeka bodza adzalephera mochititsa
manyazi.
62. Anthu a matsenga adakambirana wina ndi mnzake
pa zimene angachite ndipo adasunga zokambirana zawo.
63. Iwo adati, "Anthu awiriwa ndi anthu a matsenga amene
afuna kuti akuchotseni m'dziko lanu pogwiritsa ntchito
matsenga awo ndikugonjetsa mafumu ndi anthu anu
aulemu wawo." 64. "Motero konzekani ndipo muime mu
mzere. Iwo amene apambane lero, ndithudi, adzakhala
opambanadi."
65. Iwo adati, "Iwe Mose! Kodi udzayamba ndiwe kuponya

ndodo yako kapena tiyambe ndife kuponya ndodo zathu?”
66. Iye adati, “Iyayi. Ponyani zanu poyamba.” Ndipo
taona ndi mphamvu ya matsenga awo, zingwe ndi ndodo
zawo zidaoneka, m’maso mwa Mose, kuti zinali kuyenda
mofulumira. 67. Motero Mose adachita mantha mu mtima
mwake. 68. Koma Ife tidamuuza kuti, “Usaope! Ndithudi
iwe udzapambana.” 69. “Ndipo ponya chimene chili
m’dzanja lako la manja. Icho chidzameza zinthu zimene
iwo akonza chimene ndi chinyengo cha matsenga ndipo
munthu wa matsenga sadzapambana ngakhale atakhala
odziwa chotani.” 70. Anthu a matsenga adagwa pansi
kulambira nati, “Ife takhulupirira mwa Ambuye wa Aroni
ndi Mose.”

71. Farawo adati, “Kodi inu mukumukhulupirira iye
wopanda chilolezo changa? Ndithudi munthu uyu ayenera
kukhala mkulu wanu amene adakuphunzitsani matsenga.
Ndithudi ine ndidzadula manja anu ndi miyendo yanu
mosiyanitsa ndipo, ndithudi, ine ndidzakupachikani pa
thunthu la mtengo wa mgwalangwa. Ndipo, ndithudi, inu
mudzadziwa kuti ndani mwa ife amene akhoza kupereka
chilango chowawa kwambiri ndiponso chosatha.”

72. Iwo adati, “Ife sitifuna iwe kuposa zizindikiro zimene
zadza kwa ife ndi Iye amene adatilenga ife. Kotero iwe chita
chimene ufuna kuchita chifukwa iwe ukhoza kulamulira za
m’moyo uno zokha.” 73. “Ndithudi ife taika chikhulupiriro
chathu mwa Ambuye wathu kuti atikhululukire ife machimo
athu ndiponso pa matsenga amene udatikakamiza kuti
tichite ndipo malipiro a Mulungu ndi abwino ndiponso
osatha pofanizira ndi malipiro ako.”

74. Ndithudi! Aliyense amene adza pamaso pa Ambuye

wake ali wamachimo, ndithudi, iye adzaponyedwa ku
Gahena kumene sadzakhala ndi moyo kapena imfa.
75. Koma iye amene adza kwa Iye ndi chikhulupiriro
choonadi ndiponso ntchito zabwino, adzakhala ndi
ulemerero wapamwamba zedi. 76. Minda yamuyaya
yomwe pansi pake pamayenda mitsinje m'menemo iwo
adzakhalamo nthawi zonse. Amenewa ndiwo malipiro a
iwo amene amadziyeretsa.
77. Ndithudi Ife tidamuuza Mose kuti, "Nyamuka nthawi
yausiku pamodzi ndi akapolo anga ndipo uwatsekulire njira
pakati pa nyanja ndipo usaope kuti akupeza, kapena kumira
m'nyanja." 78. Ndipo Farawo adawatsatira ndi asirikali ake
koma madzi adawamiza onse. 79. Farawo adasocheretsa
anthu ake ndipo sadawatsogolere ayi.
80. Oh Inu ana a Israyeli! Ife tidakupulumutsani inu
kwa adani anu ndipo tidachita lonjezo ndi inu pambali
yakumanja kwa Phiri ndipo tidakutsitsirani manna ndi
mbalame zokoma. 81. Idyani zinthu zabwino zimene
tidakupatsani ndipo musaswe malamulo chifukwa mkwiyo
wanga ungagwe pa inu. Ndipo yense amene umpeza
mkwiyo wanga ndithudi watha. 82. Ndipo, ndithudi, Ine
ndimakhululukira aliyense amene alapa, akhulupirira
ndipo achita ntchito zabwino ndiponso apitiriza kuzichita.
83. "Kodi Mose chakufulumizitsa kubwera kuno ndi kusiya
anthu ako ndi chiyani?" 84. Mose adati, "Iwo ali kumbuyo
kwangaku akunditsatira. Ndadza mofulumira kwa Inu,
Ambuye, kuti musangalale." 85. Mulungu adati, "Ndithudi!
Ife tawayesa mayeso anthu ako popembedza ng'ombe
pamene iwe unachoka ndipo Msamiri wawasocheretsa."
86. Mose adabwerera kwa anthu ake ndi mkwiyo ndiponso

mwachisoni. Iye adati, "Anthu anga! Kodi Ambuye wanu
sadakulonjezeni lonjezo labwino? Kodi munaona nthawi
ya lonjezo kutalika? Kapena chinali cholinga chanu
kuti mkwiyo wa Ambuye wanu udze pa inu ndipo inu
muphwanye lonjezo lanu kwa ine?"
87. Iwo adati, "Ife sitinaphwanye lonjezo lako pa chifukwa
chathu ayi. Koma ife anatinyamulitsa katundu wa anthu,
ndolo, ndipo tinaziponya pa moto. Zimenezo ndizo
zimene Msamiri anatiuza." 88. Ndipo iye adawatulutsira
iwo chifanizo cha thupi la ng'ombe chimene chidali ndi
mawu. Iwo adati, "Uyu ndi mulungu wanu ndi mulungu
wa Mose yemwe adamuiwala." 89. Kodi iwo sanaone kuti
sichidawayankhe china chilichonse ndipo kuti chinalibe
mphamvu yowapweteka kapena kuwathandiza iwo?
90. Ndithudi Aroni adawauza iwo poyamba kuti, "Oh
Anthu anga! Inu muli kungoyesedwa nacho ichi koma,
ndithudi, Ambuye wanu ndiye Mwini chisoni chosatha
motero tsatireni ine ndipo mverani malamulo anga." 91. Iwo
adati, "Ife sitidzasiya kuchipembedza ichi mpaka pamene
Mose adza kwa ife."
92. Mose adati, "Oh Aroni! Kodi chidakuletsa ndi chiyani
kuwatsutsa iwo pamene udaona kuti ali kusochera?"
93. "Kuti siunanditsatire ine. Kodi waswa lamulo langa?"
94. Aroni adati, "Mwana wa Amayi anga! Usandikoke ndevu
zanga kapena tsitsi langa! Ndithudi! Ine ndidali ndi mantha
kuti mwina iwe ukhoza kudzanena kuti, iwe wabzala
mpatuko pakati pa ana a Israyeli ndipo siunalemekeze mau
anga."
95. Mose adati, "Iwe Msamiri, kodi chifukwa chiyani
udachita izi?" 96. Iye adati, "Ine ndidaona zimene iwo sanali

kuona. Motero ine ndidatenga dothi lodzala m'manja
kuchokera ku fumbi lochokera ku phazi la Mtumwi ndi
kulitaya. Kotero mzimu wanga udandikakamiza." 97. Mose
adati, "Choka! Ndithudi chilango chako m'moyo uno ndi
chakuti udzanena kuti, 'Musandikhudze.' Ndithudi iwe
uli ndi lonjezo limene siliphwanyidwa ayi. Taona mulungu
wako amene wamutumikira ndi mtima wako wonse. Ife
tidzaliotcha m'moto ndipo tidzamwaza phulusa lake pa
nyanja." 98. Mulungu wanu ndi Mulungu mmodzi yekha.
Iye amadziwa chilichonse.

99. Kotero Ife tili kukufotokozerani mbiri ya zinthu
zimene zidachitika kale. Ndithudi takupatsa chikumbutso.
100. Iwo amene adzachikana ndithudi adzanyamula katundu
wolemera wamachimo pa tsiku la kuuka kwa akufa. 101. Iwo
adzakhala m'menemo mpaka kalekale ndipo zidzakhala
zoipa kwambiri kwa iwo osenza katundu wotereyu tsiku
la kuuka kwa kufa. 102. Tsiku limene lipenga lidzaimbidwa,
patsiku limene Ife tidzasonkhanitsa anthu onse ochimwa,
maso awo adzakhala obiriwira ndi nkhope zakuda.
103. Monong'onezana adzakhala ali nkuyankhulana nati,
"Inu simunakhale padziko lapansi kupatula masiku khumi
okha." 104. Ife tili kudziwa kwambiri zimene adzayankhula,
pamene anthu awo angwiro ndi anzeru adzati, "Inu
simunakhale padziko kupatula tsiku limodzi lokha."

105. "Ndipo iwo ali kukufunsa za mapiri. Nena, "Ambuye
wanga adzawachotsa iwo ndi kuwamwaza ngati fumbi la
dothi." 106. "Ndipo iye adzawasiya kukhala ngati bwalo
lasesese." 107. "M'menemo sudzaona malo otsika kapena
okwera." 108. Pa tsiku limeneli, anthu adzatsatira woitana
wa Mulungu, mopanda chinyengo. Ndipo mawu onse

adzachepetsedwa chifukwa cha Mwini chisoni ndipo iwe siudzamva china kupatula mgugu wochepa wa mapazi awo.

109. Patsiku limeneli, palibe wina amene adzakhala ndi mphamvu yoyankhula m'malo mwawo kupatula yekhayo amene adzalandire chilolezo cha Mwini chisoni ndiponso amene mawu ake ngolandiridwa kwa Iye. 110. Amadziwa zonse zimene zili kutsogolo kwawo ndiponso zimene zili kumbuyo kwawo ndi zimene zili nkudza pamene iwo sadziwa china chilichonse cha Iye. 111. Ndipo nkhope zonse zidzachepetsedwa pamaso pa Mwini moyo wa nthawi zonse amene amateteza china chilichonse. Ndipo yense amene analakwa, ndithudi, ndi olephera. 112. Ndipo iye amene achita ntchito zabwino ndipo ndi munthu wokhulupirira, iye sadzaopa kuponderezedwa kapena kumanidwa malipiro.

113. Motero Ife tidatumiza Korani mu Chiarabu ndipo tafotokoza m'menemo mowirikiza machenjezo kuti iwo akhale oopa Mulungu kapena kuti Koraniyo iwapatse chiphunzitso kuchokera mu ilo. 114. Wolemekezeka ndi Mulungu, Mfumu ya choonadi! Ndipo usafulumire kulakatula Korani, chivumbulutso chake chisanathe koma uyenera kunena kuti, "Ambuye ndionjezereni nzeru."

115. Ndithudi Ife tidachita lonjezo ndi Adamu kale koma iye adaiwala ndipo sitinapeze chipiriro kwa iye. 116. Pamenepo Ife tidawauza angelo kuti, "Mugwadireni Adamu." Ndipo onse adamugwadira koma Satana adakana. 117. Ife tidati, "Oh iwe Adamu! Ndithudi uyu ndi mdani wako ndiponso mdani wa mkazi wako. Musalole kuti akutulutseni ku Paradiso ndi kukukhazikani m'mavuto."

118. Ndithudi muli ndi lonjezo lathu kuti kumeneko

inu simudzamva njala kapena kukhala wamaliseche.
119. Ndiponso inu simudzamva ludzu m'menemo kapena
kutentha kwa dzuwa. 120. Koma Satana adamunong'oneza
nati, "Oh iwe Adamu! Kodi ndingakulangize mtengo wa
moyo wosatha ndiponso ufumu wosatha?" 121. Ndipo onse
adadya chipatso cha mumtengo uja kotero udaonekera
umaliseche wawo ndipo adayamba kudziveka masamba
a m'munda muja. Kotero Adamu adanyoza lamulo la
Ambuye wake ndipo adasochera. 122. Ndipo Ambuye
wake adamusankha iye ndipo adamukhululukira ndi
kumutsogolera kunjira yoyenera.

123. Mulungu adati, "Chokani inu m'menemo, nonse
awiri, ndipo inu mudzakhala adani a wina ndi mnzake.
Pamene ulangizi wanga udzavumbulutsidwa kwa inu, iye
amene adzautsatira sadzasochera kapena kuona mavuto."
124. "Koma iye amene safuna kumvera machenjezo anga,
ndithudi, adzakhala movutika ndipo tidzamuukitsa
ali wakhungu pa tsiku louka kwa akufa." 125. Iye adzati,
"Ambuye wanga! Bwanji mwandiukitsa wakhungu, pamene
ine ndidali wopenya?" 126. Mulungu adzati, "Chifukwa
chakuti pamene chivumbulutso chathu chinadza kwa
iwe udachiiwala. Chimodzimodzi tsiku lino nawenso
waiwalidwa." 127. Mmenemu ndi mmene timalipirira munthu
oswa malamulo amene sakhulupirira chivumbulutso cha
Ambuye wake. Koma chilango cha m'moyo umene uli
nkudza ndi choopsa ndiponso chosatha.

128. Kodi iwo saona mibadwo ya anthu imene tidaiononga
iwo asanadze? Iwo amayenda pakati pa nyumba zimene iwo
anali kukhalamo. Ndithudi mu zimenezi muli zizindikiro
kwa anthu a nzeru. 129. Akadakhala kuti Ambuye wako

sadalonjeze ndi kukhazikitsa nthawi, chilango chawo
chikanadza kale. 130. Motero pirira pa zimene ali kunena
ndipo lemekeza ndi kutamanda Ambuye wako dzuwa
lisanatuluke ndiponso lisanalowe. Ndipo muyamike Iye
nthawi yausiku ndi yausana kuti iwe udzasangalale.

131. Usasirire zinthu zimene tawapatsa anthu chifukwa
zimenezi ndi zosangalatsa za m'moyo uno. Ife tingofuna
kuwayesa nazo. Koma mphotho ya Ambuye wako ndi
yabwino ndipo ndi yosatha. 132. Ndipo lamulira banja
lako kupemphera ndipo ukhale wopirira pokwaniritsa
mapemphero. Ife sitipempha zinthu kwa iwe koma Ife
timakupatsa zofuna zako. Ndipo mapeto abwino ndi a
anthu oopa Mulungu.

133. Iwo adati, "Bwanji iye satipatsa ife chizindikiro
chochokera kwa Ambuye wake?" Kodi iwo sadapatsidwe
zizindikiro zambiri zimene zili m'mabuku a kale a
Mulungu? 134. Ngati Ife tikadawaononga iwo ndi chilango
tisadawatumizire ichi, iwo akadati, "Ambuye wathu! Inu
mukadatitumizira Mtumwi, ndithudi, ife tikadatsatira
chivumbulutso chanu tisadanyozedwe ndi kuchititsidwa
manyazi." 135. Nena, "Onse ali kudikira. Nanunso dikirani
ndipo inu mudzadziwa kuti ndani amene adatsatira njira
yoyenera ndiponso amene ali otsogozedwa."

# Al-Anbiya

M'dzina la Mulungu, Mwini chifundo ndi Mwini chisoni chosatha.

1. Chayandikira kwa anthu chiweruzo cha ntchito yawo
ndi pamene iwo abwerera m'mbuyo monyoza. 2. Palibe
chenjezo limene limadza kuchokera kwa Ambuye wawo
limene iwo amalimvera kupatula pamene iwo ali kusewera.
3. Ndi mitima yotangwanika, iwo amene amachita zoipa
amauzana mwamseri kuti, "Kodi uyu si munthu ngati inu?
Kodi inu mukutsatira matsenga pamene muli kuona?"
4. Iye adati: "Ambuye wanga amadziwa chilichonse chimene
chimanenedwa kumwamba ndi pa dziko lapansi ndipo
Iye amamva zonse ndiponso amadziwa chinthu china
chilichonse."

5. Koma ena amati, "Ichi si china koma maloto a bodza!
Iyayi! Iye walipeka. Iyayi, iye ndi mlakatuli! Ndipo
mulekeni atilangize ife chizindikiro china monga momwe
Atumwi akale ankachitira." 6. Palibe umodzi wa mizinda
imene tidaononga imene idakhulupirira iwo asanadze.
Kodi iwo adzakhulupirira?

7. Ndipo Ife, iwe usadabwere sitidatumize ena, koma
amuna omwe timawapatsa chivumbulutso. Motero afunse
anthu ozindikira ngati iwe siudziwa. 8. Ife sitidawapange
iwo ndi matupi amene samadya chakudya kapena amuyaya
ayi. 9. Ndipo Ife tidakwaniritsa lonjezo lathu kwa iwo,

ndipo tidawapulumutsa iwo pamodzi ndi ena amene Ife
tidawafuna koma tidaonongeratu anthu onse ochimwa.
10. Ndithudi tavumbulutsa Buku m'mene muli
chikumbutso kwa inu. Kodi mulibe nzeru? 11. Kodi ndi
mizinda ingati imene tidaononga imene idali yochita
zoipa, ndipo m'malo mwawo tidaikamo anthu ena?
12. Ndipo pamene iwo adaona chilango chathu iwo adayesa
kuthawa m'mizinda yawo. 13. "Musathawe koma bwererani
kumene mumakhala moyo wa chisangalalo ndi ku nyumba
zanu kuti mukafunsidwe." 14. Iwo anati, "Tsoka kwa ife!
Ndithudi tinali kuchita zoipa." 15. Koma kulira kwawo
sikunathe mpaka pamene Ife tidawaononga ndi kukhala
ngati munda umene wakololedwa.
16. Sitidalenge mwamasewera kumwamba ndi dziko lapansi
ndi zonse zimene zili pakati pake. 17. Ife tikadafuna kuti
tisangalale tikadadzipangira tokha, ngati Ife tikadafunadi
kutero. 18. Iyayi! Ife timatumiza choonadi kuti chilimbane
ndi bodza ndipo chimalionongа. Taonani, ilo latha. Ndipo
tsoka kwa inu chifukwa cha zimene mumanena.
19. Zake ndi zonse zimene zili kumwamba ndi pa
dziko lapansi. Ndipo onse amene ali pafupi pake
sanyozera kumupembedza Iye ndipo satopa ayi. 20. Iwo
amamutamanda Iye masana ndi usiku ndipo sachita ulesi.
21. Kodi iwo asankha milungu ya pa dziko lapansi imene
imadzutsa anthu akufa? 22. Kukadakhala milungu ina
kumeneko yoonjezera pa Mulungu weniweni, ndithudi,
konse kukadaonongeka. Alemekezeke Mulungu, Mwini
wa Mpando wa Chifumu, mu zimene akumunenera. 23. Iye
sangafunsidwe pa ntchito zimene amachita pamene iwo
adzafunsidwa.

24. Kodi kapena iwo asankha milungu ina yoonjezera pa
Mulungu weniweni? Nena, "Bweretsani umboni wanu".
Ichi ndi chikumbutso cha amene ndili nawo ndiponso iwo
amakedzana. Koma ambiri a iwo sadziwa choonadi motero
salabadira. 25. Ndipo Ife sitidatumize iwe usadabadwe,
Mtumwi wina aliyense amene sitinamuuze kuti, "Kulibe
Mulungu wina koma Ine ndekha, kotero ndi pembedzeni
Ine."
26. Iwo amati, "Mwini chisoni chosatha wabereka
mwana wamwamuna." Iye alemekezedwe! Amenewo si
ena ayi koma akapolo ake olemekezeka. 27. Iwo sayankhula
pokhapokha Iye atayankhula, ndipo amachita zinthu
potsatira malamulo ake. 28. Iye amadziwa zonse zimene zili
patsogolo pawo ndiponso zimene zili m'mbuyo mwawo
ndipo iwo sangalankhulire wina aliyense chipulumutso
kupatula amene Iye wamukonda ndipo iwo amanjenjemera
chifukwa cha mantha pomuona Iye. 29. Ndipo ngati wina wa
iwo atanena kuti, "Ndithudi ine ndine mulungu kuonjezera
pa Iye." Oteroyo adzalangidwa ndi moto wa ku Gahena.
Mmenemo ndi mmene timalipirira anthu olakwa.
30. Kodi anthu osakhulupirira sadziwa kuti kumwamba
ndi dziko lapansi chidali chinthu chimodzi chogwirana
chimene tidachisiyanitsa? Ndipo tidapanga, chilichonse
chamoyo, kuchokera ku madzi. Kodi iwo sangakhulupirire?
31. Ndipo Ife tidakhazikitsa mapiri pa dziko lapansi
molimba kuti asagwedezeke pamodzi ndi iwo ndipo
tidakhazikitsa misewu pa miyala kuti mwina atsogozedwe.
32. Ndipo tidapanga kumwamba denga losungika bwino
limene silingagwe. Komabe iwo amakana zizindikiro
zake. 33. Iye ndiye amene adalenga usiku ndi usana, dzuwa

ndi mwezi ndi china chilichonse chimene chimayenda
mlengalenga.
34. Palibe munthu, pambuyo pako amene tidamulenga kuti
sadzafa. Ngati iweyo udzafa, kodi iwo adzakhala ndi moyo
mpaka kalekale? 35. Chilichonse cholengedwa chidzalawa
imfa ndipo Ife tidzakuyesani ndi zinthu zoipa ndi zabwino
ndipo ndi kwa Ife kumene nonse mudzabwerera.
36. Pamene anthu osakhulupirira amakuona iwe,
sakuganizira zabwino koma chipongwe ndipo amati, "Kodi
uyu ndiye munthu amene amayankhula zoipa za milungu
yanu?" Pamene iwo amakana zonse zokhudza Mwini
chisoni chosatha.
37. Munthu adalengedwa kukhala opupuluma pochita
zinthu. Ine ndidzakusonyezani zizindikiro zanga. Motero
musandifulumizitse. 38. Iwo amati, "Kodi lonjezo limeneli
lidzakwaniritsidwa liti ngati zimene uli kunena ndi
zoona?" 39. Akadadakhala kuti anthu osakhulupirira akudziwa
tsiku limene iwo sadzakhala ndi mphamvu zophimba
nkhope kapena misana yawo kudziteteza ku moto ndipo
iwo sangathandizike. 40. Iyayi. Ilo lidzadza kwa iwo
mwadzidzidzi ndipo adzadodoma ndi kusokonezeka ndipo
iwo sadzatha kulibweza ndiponso sadzapatsidwa nthawi
yopuma. 41. Ndithudi Atumwi ena, adachitidwa chipongwe
kale, koma anthu a chipongwe adafafanizidwa ndi chilango
chimene iwo adachichitira chipongwe.
42. Nena, "Kodi ndani adzakutetezani inu nthawi ya usiku
ndi nthawi ya masana ku mkwiyo wa Mwini chisoni?"
Komabe iwo salabadira zokumbukira Ambuye wawo.
43. Kapena iwo ali ndi milungu ina yoti ingawateteze

kwa Ife? Iyo siingathe kudziteteza yokha; ndiponso iwo
sangatetezedwe kuchilango chathu.
44. Koma Ife tidapereka zokoma za m’moyo uno kwa
anthuwa pamodzi ndi makolo awo mpaka pamene nthawi
idawatalikira iwo. Kodi iwo saona kuti Ife timachepetsa
dziko lawo kuchokera m’malire mwake? Kodi iwo ndiwo
adzapambane?
45. Nena, “Ine ndili kukuchenjezani ndi chivumbulutso,
koma agonthi sadzamva kuitana pamene achenjezedwa.
46. Koma ngati katsoka kakang’ono kochokera kwa Ambuye
wako kagwa pa iwo, ndithudi, iwo adzalira, “Tsoka kwa ife;
ndithudi tidali anthu ochita zoipa.”
47. Ndipo Ife tidzakhazikitsa miyeso yoyenera pa tsiku
la kuuka kwa akufa ndipo aliyense sadzaponderezedwa pa
china chilichonse. Ngakhale patakhala ntchito zazing’ono
zolingana ngati kanthangala kakang’ono tidzazitulutsa kuti
ziyesedwe. Ndipo Ife ndife okwana kuwerengera ntchito
zonse.
48. Ndithudi Ife tidamupatsa Mose ndi Aroni muyeso ndi
muuni wowala ndi chikumbutso kwa anthu angwiro. 49. Iwo
amene amaopa Ambuye kuchokera m’maganizo a pansi
penipeni pa mtima ndipo amaopa tsiku louka kwa akufa.
50. Ndipo ichi ndi chivumbulutso chodalitsika chimene
tatumiza. Kodi mudzachikana?
51. Ndithudi Ife tidamupatsa kale chilangizo Abrahamu
ndipo tinali kumudziwa bwino. 52. Pamene Iye adawauza
abambo ake ndiponso anthu ake kuti, “Kodi mafano
amene muli kuwapembedzawa ndi chiyani?” 53. Iwo adati,
“Ife tidapeza makolo athu ali kuwapembedza.” 54. Iye

adati, “Ndithudi inu ndiponso makolo anu mwakhala muli
kuchimwa kwambiri.”
55. Iwo adati, “Kodi ndi zoona zimene wadza nazo kwa ife
kapena ndi nthabwala chabe?” 56. Iye adati, “Iyayi. Ambuye
wanu ndi amene adalenga kumwamba ndi dziko lapansi
ndipo muzimenezo ine ndichitira umboni.” 57. “Ndilumbira
pali Mulungu kuti ine ndidzachita chiwembu pa mafano
anu inu mukangochoka.” 58. Motero iye adaziphwanya
zonse kukhala tizidutswa kupatula fano lalikulu kuti
akhoza kudzalifunsa.
59. Iwo adati: “Kodi ndani amene wachita izi kwa
milungu yathu? Ndithudi iye ali oipitsitsa.” 60. Iwo adati,
“Ife tinamva mnyamata wotchedwa Abrahamu akunena
za milunguyo.” 61. Iwo adati, “Mubweretseni pamaso pa
anthu onse kuti achitire umboni.” 62. Iwo adati, “Kodi iwe
ndi amene wachita izi ku milungu yathu? Oh Abrahamu!”
63. Iye adati, “Iyayi. Ndi uyu, wamkulu kuposa zonse amene
waziphwanya. Afunseni, ngati angayankhule”
64. Pamenepo iwo adayang’anizana okha nati, “Ndithudi
inu ndinu anthu ochimwa kwambiri.” 65. Ndipo
adayang’anizananso nati, “Ndithudi iwe uli kudziwa
kuti milungu iyi siiyankhula.” 66. Abrahamu adati, “Kodi
inu mumapembedza mowonjezera pa Mulungu zinthu
zimene sizingathe kukuthandizani chilichonse kapena
kukuonongani?” 67. “Tsoka likhale pa inu ndi pa mafano
anu amene mumapembedza kuonjezera pa Mulungu! Kodi
mulibe nzeru?”
68. Onse adati, “Mutentheni kuti muteteze milungu yanu
ngati mufuna kuchita china chilichonse.” 69. Ife tidati, “Iwe
moto khala wozizira ndi wamtendere kwa Abrahamu.”

70. Ndipo iwo adafuna kumuononga Iye koma Ife
tidawapanga iwo kukhala olephera.
71. Koma Ife tidamupulumutsa iye pamodzi ndi Loti ndipo
tidawaika ku dziko limene tidalidalitsa kuti zolengedwa
zonse zikhalemo. 72. Ndipo Ife tidamupatsa Isake ndi
Yakobo ngati chidzukulu chake ndipo tidawapanga onse
kukhala anthu angwiro. 73. Ndipo Ife tidawasankha iwo
kukhala atsogoleri olangiza anthu ku ulamuliro wathu
ndipo tidawalamulira kuti azigwira ntchito zabwino ndipo,
azipitiriza kupemphera ndi kupereka zothandizira osauka.
Ndipo iwo anali kutitumikira Ife nthawi zonse.
74. Ndi Loti tidamupatsa luntha, utumiki ndi nzeru za
chipembedzo ndipo tidamupulumutsa ku mzinda umene
anthu ake anali kuchita zoipa. Ndithudi, iwo anali anthu
ochita zoipa ndipo anali osamvera Mulungu. 75. Ndipo
Ife tidamulowetsa m’chisomo chathu, ndithudi, iye adali
mmodzi wa anthu olungama.
76. Ndi pamene Nowa adatipempha poyamba, Ife
tidamva pempho lake ndipo tidamupulumutsa iye
pamodzi ndi anthu ake ku chilango choopsa. 77. Ndiponso
Ife tidamupulumutsa ku gulu la anthu amene adakana
chivumbulutso chathu. Ndithudi iwo anali anthu oipa
ndipo onse tidawamiza m’madzi.
78. Pamene Davide ndi Solomoni adaweruza mulandu
wa munda umene nkhosa zosochera za anthu ena zidadya
nthawi ya usiku. Ndipo Ife tidali mboni pa chiweruzo chawo.
79. Ife tidapatsa Solomoni nzeru zoweruzira nkhaniyi ndipo
aliyense wa iwo tidamupatsa luntha, utumwi ndi nzeru.
Tinalamula mapiri ndi mbalame kuti zikhale pamodzi ndi
Davide pomutamanda Mulungu. Ndife amene tidachita

zonsezi. 80. Ndipo tidamuphunzitsa luso lopanga zovala za
nkhondo kuti zizikutetezani pa nthawi ya nkhondo, Kodi
ndinu othokoza?
81. Ndi Solomoni, Ife tidampeputsira mphamvu ya
mphepo. Iyo inali kuomba potsatira malamulo ake kupita
kudziko limene Ife tidalidalitsa. Ndipo Ife timadziwa
zinthu zonse. 82. Ndipo pakati pa a Satana padali ena omwe
amaimira m'malo mwa iye ndipo amachitanso ntchito zina.
Kuonjezera apa ndipo ndife amene timawayang'anira iwo.
83. Ndi Yobu pamene adaitana Ambuye wake nati, "Ine,
ndithudi, mavuto andikuta ndipo Inu ndinu wachisoni
kuposa achisoni onse." 84. Motero Ife timamuyankha
pempho lake ndipo tidamuchotsera mavuto ake ndipo
tidamubwezeranso banja lake ndi zinthu zambiri zimene
tidamupatsa ngati chisomo chochokera kwa Ife ndi
chikumbutso kwa onse amene amatipembedza Ife.
85. Ndipo Ishimayeli, Idris ndi Dhulkifl, onse adali anthu
opirira. 86. Ndipo Ife tidawalowetsa m'chisomo chathu.
Ndithudi iwo adali anthu olungama.
87. Ndi Dhan-Nun pamene adachoka mokwiya kwambiri
chifukwa iye adali kuganiza kuti Ife sitingamulenge iye.
Koma mu mdima iye adaitana, "Kulibe Mulungu wina
koma Inu nokha. Ulemerero ukhale kwa Inu! Ndithudi
ine ndidali mmodzi mwa anthu olakwa!" 88. Motero Ife
tidayankha pempho lake ndipo tidamupulumutsa ku
mavuto ake. Motero ndimo mmene timapulumutsira
anthu okhulupirira.
89. Ndi Zakariya pamene anaitana Ambuye wake nati,
"Ambuye wanga! Musandileke ndekha. Ndipo Inu ndinu
wabwino mwa okhalitsa onse." 90. Motero Ife tidamuyankha

pempho lake ndipo tidamupatsa Yohane ndipo tidathetsa
uchumba wa mkazi wake. Ndithudi iwo adali ofulumira
pochita ntchito zabwino ndipo amatipempha Ife ndi
chikhulupiriro ndi mantha ndiponso amadzichepetsa kwa
Ife.
91. Adali mkazi amene adasunga unamwali wake. Ife
tidauzira mwa iye ndipo tidamupanga iye pamodzi ndi
mwana wake wa mwamuna kukhala chizindikiro kwa
zolengedwa zonse.
92. Ndithudi! Ichi ndi chipembedzo chanu ndipo
ndi chipembedzo chimodzi, ndipo Ine ndine Ambuye
wanu motero ndipembedzeni Ine ndekha. 93. Ndipo iwo
adapatukana ndi kugawa chipembedzo chawo pakati pawo
ndipo ndi kwa Ife kumene adzabwerera. 94. Motero aliyense
amene achita ntchito zabwino ndipo ndi wokhulupirira
moona ntchito zake sizidzakanidwa ayi. Ndithudi Ife
timazilemba zonse m’Buku la chiwerengero.
95. Ndipo ndi koletsedwa kuti mudzi umene
tidawuwononga kuti ubwererenso. 96. Mpaka pamene
anthu a Ya-juj ndi Majuj adzamasulidwa ndipo iwo
adzakhala akutsika kuchokera kumalo aliwonse wokwera.
97. Ndipo pamene lonjezo loona lidzafika, maso a anthu
onse osakhulupirira adzapenyetsetsa mwamantha nati
“Tsoka kwa ife! Ndithudi ife tidali osalabadira zimenezi.
Zoonadi ife tidali ochita zoipa.”
98. Ndithudi! Inu pamodzi ndi zimene mukupembedza
kuonjezera pa Mulungu, mudzakhala nkhuni za ku Gahena!
Kumeneko nonse mudzalowako. 99. Iyo ikadakhala
milungu, siikadalowa kumeneko ndipo onse adzakhala
kumeneko. 100. Kumeneko iwo adzalira ndipo adzakhala

osamva. 101. Ndithudi iwo amene tawaonetsera chifundo
chathu, iwo adzakhala kutali ndi moto. 102. Iwo sadzamva
mkokomo wake pamene iwo ali kumene mitima yawo
imafuna mpaka kalekale. 103. Zoopsa sizidzawadandaulitsa
ayi ndipo Angelo adzawalandira iwo nati,"Ili ndi tsiku lanu
limene inu mudalonjezedwa."

104. Tsiku limene tidzapinde thambo monga
momwe timapindira tsamba la Buku. Monga momwe
tidayamba chilengedwe choyamba momwemonso
tidzachibwezeranso. Ili, ndithudi, ndi lonjezo kwa Ife.
Ndithudi, Ife, tidzachita motero. 105. Ndipo, ndithudi, Ife
tidalemba m'Buku la Masalimo, motsatira chikumbutso
kuti akapolo anga angwiro adzakhala ku dziko lapansi.
106. Ndithudi mu ili muli Uthenga womveka kwa anthu
amene amapembedza Mulungu.

107. Ndipo sitidakutumize iwe pa chifukwa china
koma ngati madalitso kwa zolengedwa zonse. 108. Nena,
"Zavumbulutsidwa kwa ine kuti Mulungu wanu ndi
mmodzi yekha. Kodi inu mudzadzipereka kwa Iye?"
109. Koma ngati iwo safuna kumvera nena, "Ine ndili
kukuchenjezani kuti tonse tidziwe. Ine sindidziwa kuti
chimene mwalonjezedwa chidza msanga kapena chikadali
patali." 110. Ndithudi Mulungu amadziwa zonse zimene
mumayankhula mokweza ndipo amadziwanso zimene
mubisa. 111. Ndipo ine sindidziwa ngati awa ndi mayeso kwa
inu ndi chisangalalo cha kanthawi kochepa. 112. Iye anati,
"Ambuye wanga! Weruzani mwachilungamo! Ambuye
wathu ndi Mwini chisoni chosatha amene chithandizo
chake chimafunika pa zimene inu muonjezera."

# Al – Haj

M'dzina la Mulungu, Mwini chifundo ndi Mwini
chisoni chosatha.

1. Oh anthu inu! Opani Ambuye wanu ndipo kwaniritsani
udindo wanu kwa Iye. Ndithudi chivomezi cha
nthawiyo chidzakhala choopsa kwambiri. 2. Tsiku limene
mudzachiona, mkazi aliyense woyamwitsa adzaiwala
mwana wake ndipo mkazi aliyense wapakati adzabala
nthawi yake isanafike ndipo udzawaona anthu ngati
oledzera pamene sali oledzera; koma chilango cha
Mulungu chidzakhala chowawa. 3. Ndipo pakati pa anthu
pali ena amene amatsutsa za Mulungu pamene sazidziwa,
ndipo amatsatira Satana aliyense ogalukira. 4. Kwa iye,
zidalamulidwa kuti aliyense amene amutsatira iye,
adzamusocheretsa ndipo adzamupititsa ku chilango cha
ku ng'anjo ya moto.
5. Oh anthu inu! Ngati inu mukayika za kuukanso kwa
akufa, ndithudi, Ife tidakulengani kuchokera ku dothi,
ndi kudontho la umuna, losakanizana ndi ukazi ndiponso
kuchokera ku mnofu oumbidwa bwino osonyeza ziwalo za
munthu ndi wina mnopfu umene siunayambe kusonyeza
ziwalo kuti tikusonyezeni mphamvu zathu. Ndipo Ife
timakhazikitsa m'chiberekero cha mkazi chilichonse
chimene tifuna panthawi yomwe yaikidwa ndipo
timakutulutsani ngati makanda ndipo mumakula kufika
pa msinkhu waumunthu. Ndipo ena a inu amafa ndipo

ena amabwezeredwa moyo wapansi kuti asadziwe zonse
zimene anali kudziwa kale. Ndipo inu mumaona nthaka
ili youma yosamera chilichonse koma tikatsitsa madzi
panthakapo, iyo imayamba kugwedezeka ndi kutupa
ndi kumeretsa mbewu zokongola zamitundumitundu.
6. Zimenezo ndi chifukwa chakuti Mulungu ndiye choonadi
ndipo Iye amapereka moyo ku zinthu zakufa ndipo ali ndi
mphamvu pa chinthu china chilichonse. 7. Ndithudi ola lili
nkudza mosakayika pamene Mulungu adzawadzutsa onse
amene ali m'manda.

8. Ndipo pakati pa anthu pali wina amene amatsutsa
za Mulungu pamene sakudziwa chilichonse ndiponso
chilangizo kapena Buku la chivumbulutso. 9. Munthu
wotere amathyola khosi monyadira ndi kusocheza ena ku
njira ya Mulungu. Kwa otere kuli mnyozo m'moyo uno
ndipo patsiku louka kwa akufa, tidzamulawitsa chilango
cha moto woyaka. 10. "Izi ndi chifukwa cha zomwe manja
anu adatsogoza ndipo, ndithudi, Mulungu sapondereza
akapolo ake.

11. Ndipo pakati pa anthu pamakhala munthu amene
amampembedza Mulungu mokayikira. Zikapezeka
zabwino amakhala wokhutitsidwa ndi izo koma ngati
mavuto amugwera amatembenuka motero; iye amataya
zabwino za m'moyo uno ndi za m'moyo umene uli nkudza.
Kumeneko ndiko kulephera koonekeratu.

12. Iwo amapempha mowonjezera pa Mulungu, zimene
sizingathe kumuononga kapena kumuthandiza. Kumeneko
ndiko kusochera kwenikweni. 13. Amapempha kwa iye
amene mavuto ake ali pafupi kuposa chithandizo chake.
Iye, ndithudi, ndi mtsogoleri woipa ndiponso bwenzi

loipa. 14. Ndithudi Mulungu adzawalowetsa onse amene
amakhulupilira ndipo amachita ntchito zabwino m'minda
yothiriridwa ndi mitsinje ndi madzi oyenda. Ndithudi
Mulungu amachita zimene afuna.
15. Ngati wina aganiza kuti Mulungu sadzathandiza
Mtumwi wake m'dziko lino ndi m'dziko limene lili nkudza,
mulekeni amange chingwe ku phaso la nyumba yake
ndi kudzimangirira yekha. Ndipo mulekeni kuti awone
yekha ngati cholinga chake chingachotse vuto lomwe
limamukwiyitsa iye. 16. Kotero Ife talitumiza ilo ngati
zizindikiro zooneka ndipo ndithudi Mulungu amatsogolera
aliyense amene Iye wamufuna.
17. Ndithudi iwo amene amakhulupirira, ndi iwo amene
ndi Ayuda, Masabina, Akhirisitu, a Magiyani ndi akunja,
ndi iwo amene amapembedza zinthu zina mowonjezera
pa Mulungu. Ndithudi, Mulungu adzawaweruza pa tsiku
la kuuka kwa akufa ndipo Mulungu ndi mboni pa zinthu
zonse.
18. Kodi iwe siudaone kuti zinthu zonse zimalambira
Mulungu mwachitsanzo zinthu zimene zimakhala
kumwamba ndi padziko lapansi monga dzuwa, mwezi,
nyenyezi, mapiri mitengo, nyama ndi anthu ambiri? Koma
pali ambiri amene chilango ndi chowayenera. Aliyense
amene achititsidwa manyazi ndi Mulungu, palibe wina
amene angamulemekeze. Ndithudi! Mulungu amachita
zimene afuna.
19. Awa awiri otsutsana, akutsutsana za Ambuye wawo
ndipo akakhala sakhulupirira Mulungu, adzawasokera
zovala za ku moto ndipo madzi ogaduka adzathiridwa
paliombo pawo. 20. Ndi iwo zidzasungunuka zonse zimene

zili m'mimba mwawo ndi pa makungu pawo. 21. Iwo
adzamangidwa ku unyolo wa zitsulo. 22. Nthawi iliyonse
imene azidzafuna kuti athawe m'menemo, chifukwa
chaululu, azidzabwezedwa momwemo ndipo adzauzidwa
kuti, "Lawani chilango chamoto."

23. Ndithudi Mulungu adzawalowetsa anthu okhulupirira
ndi ochita ntchito zabwino, m'minda yothiririridwa ndi
mitsinje yoyenda. Iwo adzavekedwa zibangiri za golide
ndi mphete za nkhombe ndipo zovala zawo zidzakhala za
silika. 24. Iwo ndi otsogozedwa ndi mawu abwino ndipo
adatsogozedwa ku njira ya Iye amene ayenera kutamandika
kwambiri.

25. Ndithudi! Iwo amene sakhulupirira ndipo amaletsa
anzawo kutsatira njira ya Mulungu ndi kupita ku Mzikiti
Woyera umene tidaupereka kwa anthu a mitundu yonse,
kaya ndi eni dziko kaya ndi alendo chimodzimodzi ngati
amachita zoipa m'kati mwake, tidzamulawitsa chilango
chowawa.

26. Ndi pamene tidamulangiza Abrahamu malo omangapo
Mzikiti Woyera tidamuuza kuti, "Usapembedze wina
aliyense koma Ine ndekha. Ndipo yeretsa nyumba yanga
kuti izikhala yaukhondo chifukwa cha anthu amene
amayenda kuizungulira iyo ndi iwo amene amaimirira
kapena amagwada ndi kuwerama popembedza."

27. Ndipo uza anthu onse kupita ku Hajji. Iwo adzadza
kwa iwe poyenda ulendo wapansi kapena atakwera
ngamira yowonda chifukwa chakutopa ndipo iwo adzadza
kuchokera kumbali zonse za kutali ndi njira za m'mapiri.
28. Kuti adzaona zinthu zimene zili zaphindu kwa iwo
ndi kutchula dzina la Mulungu, pa masiku osankhidwa,

pa nyama ya ng'ombe imene Iye wawapatsa iwo. Idyani
gawo lina ndiponso dyetsani osauka amene ali pa mavuto.
29. Aloleni kuti amalize miyambo yofunika ndi kukwaniritsa
malonjezo awo ndiponso kuzungulira Nyumba ya
Makedzana.
30. Izi zikhale choncho. Ndipo aliyense amene alemekeza
miyambo yolemekezeka ya Mulungu zidzakhala zabwino
kwa iye pamaso pa Ambuye wake. Nyama ya ng'ombe,
ndi yololedwa kwa inu kupatula nyama zokhazo zimene
zikutchulidwa kwa inu kukhala zoletsedwa. Pewani
zonyansa za mafano, ndipo pewani bodza.
31. Musapembedze wina aliyense koma Mulungu ndipo
musatumikire milungu ina. Aliyense amene amatumikira
milungu ina yoonjezera pa Mulungu weniweni, ali ngati
iye amene agwa kuchokera kumwamba, ndipo asanagwe
pansi, amalandiridwa ndi mbalame kapena kunyamulidwa
ndi mphepo kukam'taya kumalo akutali.
32. Zimenezi zili tero. Aliyense amene amalemekeza
zizindikiro za Mulungu kumeneko ndiko kuyera mtima.
33. Mu izo muli zokoma zosiyanasiyana mpaka pa nthawi
imene yaikidwa ndipo pomaliza zimaperekedwa ngati
nsembe ku Nyumba ya Makedzana.
34. Ku mtundu uliwonse, Ife tidakhazikitsa miyambo
yachipembedzo kuti azitchula dzina la Mulungu pa nyama
zimene Iye adawapatsa iwo ngati chakudya. Ndipo Mulungu
wanu ndi Mulungu mmodzi yekha motero muzigonjera Iye
yekha. Auzeni nkhani yabwino anthu onse odzichepetsa.
35. Anthu amene mitima yawo imadzala ndi mantha pamene
Mulungu atchulidwa ndiponso amene amapilira pamavuto

amene awapeza ndipo amapitiriza mapemphero awo ndi
kupereka zina za zimene tidawapatsa.
36. Ndi nyama zina tidazipanga kukhala ngati zina mwa
zizindikiro za Mulungu ndipo mwa izo muli zofunika
kwambiri kwa inu. Motero tchulani dzina la Mulungu pa
izo pamene muziika kuti ziperekedwe nsembe. Ndipo
zikaphedwa, idyani nyama yake ndiponso mumudyetse
wopempha ndi amene apempha mwamanyazi. Kotero
Ife nyamazi tazipereka kwa inu kuti mukhale othokoza.
37. Si mnofu wawo kapena magazi awo amene amafika kwa
Mulungu koma ndi kumvera Mulungu kumene kumafika
kwa Iye. Kotero Ife tazilamula kuti zizikutumikirani kuti
muzilemekeza Mulungu chifukwa chokulangizani inu njira
yoyenera. Auze nkhani yabwino anthu angwiro.
38. Ndithudi Mulungu amatchinjiriza anthu okhulupirira.
Ndithudi Iye sakonda anthu a chinyengo ndiponso
osathokoza. 39. Chilolezo chomenya nkhondo chili
kuperekedwa kwa iwo amene aputidwa, chifukwa chakuti
awachimwira. Ndithudi Mulungu ali ndi mphamvu
yowapambanitsa. 40. Anthuwo ndi amene apirikitsidwa
kuchokera ku nyumba zawo mopanda chilungamo chifukwa
chakuti iwo anati, "Ambuye wathu ndi Mulungu." Ndipo
Mulungu akadapanda kuyesa anthu ena ndi mphamvu za
anthu anzawo makachisi, matchalitchi, masunagoge ndi
mizikiti imene dzina la Mulungu limatchulidwa kwambiri
ikadaonongekeratu. Ndithudi Mulungu adzathandiza
amene amathandiza chipembedzo chake. Ndithudi
Mulungu ndi mphamvu ndiponso Wopambana kwambiri.
41. Iwo amene tawapatsa mphamvu padziko lapansi
adzapitiriza mapemphero nthawi zonse ndi kupereka

msonkho wothandiza osauka, ndipo adzakhazikitsa
chilungamo ndi kuletsa zoipa. Kwa Mulungu ndiko kuli
mapeto a zinthu zonse.
42. Ndipo ngati akukana iwe, ndithudi asanadze awa,
nawonso anthu a Nowa, Aad ndi Thamud adakana Atumwi
awo. 43. Ndiponso anthu a Abrahamu ndi anthu a Loti
zidali choncho. 44. Ndi anthu okhala ku Midiyani. Mose
nayenso adakanidwa. Koma Ine ndidawapatsa nthawi
anthu osakhulupirira ndipo pomaliza chilango changa
chidawapeza onse. Kodi chilango changa chidali choopsa
bwanji?
45. Kodi ndi mizinda ingati ya anthu ochita zoipa
imene taononga? Mizinda yawo idaonongeka, madenga
ake kugwera pansi ndiponso ndi zitsime zingati zimene
zidangokhala kusowa anthu otungapo madzi ndiponso ndi
nyumba zingati zomangidwa bwino zimene zidasanduka
mabwinja? 46. Kodi iwo sanayende pa dziko kuti mitima
yawo ikhale yozindikira ndi makutu awo kuti amvere?
Ndithudi si maso awo amene ali ndi khungu, koma ndi
mitima imene ili mu zifuwa zawo imene ili ndi khungu.
47. Ndipo ali kuuza iwe kuti ufulumizitse chilango! Ndipo
Mulungu salephera kukwaniritsa lonjezo lake. Ndithudi
tsiku lililonse kwa Mulungu lili ngati zaka chikwi chimodzi
mu kuwerenga kwanu. 48. Ndi mizinda ingati imene
ndidaipatsa mwayi wa nthawi pamene iyoyo inali kuchitabe
zoipa? Ndipo pambuyo pake ndidaipatsa chilango Kwa Ine
zinthu zonse zidzabwerera.
49. Nena, "Oh anthu inu! Ndithudi ine ndatumizidwa
ngati mchenjezi wanu!" 50. Motero iwo amene akhulupirira
ndi kuchita ntchito zabwino, adzakhululukidwa machimo

awo ndi kulipidwa mphotho yolemekezeka. 51. Koma iwo
amene amalimbikira kutsutsa zizindikiro zathu, adzakhala
eni ake a ku Gahena.
52. Ife sitidatumizepo Mtumwi kapena Mneneri, iwe
usanadze, koma iye amati akamalakatula chivumbulutso
kapena kulalikira, Satana anali kuonjezera bodza. Koma
Mulungu amachotsa zonse zimene Satana waikamo.
Motero Mulungu amakhazikitsa chivumbulutso chake
ndipo Mulungu ndi wodziwa ndi waluntha. 53. Kuti Iye
apange zimene wanena Satana kukhala mayesero kwa iwo
amene m'mitima mwawo muli matenda ndi amene mitima
yawo ndi youma. Ndithudi anthu ochita zoipa amatsutsa
kwambiri choonadi. 54. Ndipo kuti iwo amene adapatsidwa
nzeru azindikire kuti ichi ndi choonadi chochokera kwa
Ambuye wako ndipo ayenera kukhulupirira ndi kuti mitima
yawo ikhale yodzichepetsa chifukwa cha iyo. Ndithudi
Mulungu ndi Mtsogoleri wa iwo amene akhulupirira njira
yoyenera.
55. Ndipo anthu osakhulupirira adzapitirira kukayikira
chivumbulutso mpaka pamene ora lomaliza lidzawapeza
mwadzidzidzi kapena mpaka pamene chilango cha tsiku
louka kwa akufa chidzawadzera. 56. Ufumu, patsiku
limeneli, udzakhala wa Mulungu yekha. Iye adzaweruza
pakati pawo. Motero onse amene adakhulupirira ndipo
amachita ntchito zabwino adzakhala ku Paradiso. 57. Ndipo
iwo amene sanakhulupirire ndipo amakana zizindikiro
zathu chawo chidzakhala chilango chochititsa manyazi.
58. Iwo amene adasamuka kwawo chifukwa chofuna
kukweza chipembedzo cha Mulungu ndipo pambuyo pake
adaphedwa kapena adafa, Mulungu, ndithudi, adzawapatsa

mphatso zabwino. Ndithudi Mulungu ndi wopereka zabwino kuposa onse amene amapereka.
59. Ndithudi Mulungu adzawalowetsa iwo ku malo amene adzasangalala nawo ndipo Mulungu, ndithudi, ndi wodziwa zonse ndiponso wopirira kwambiri.

60. Izo zili tero. Ndipo aliyense amene abwezera mnzake chilango chofanana ndi chimene iye wapatsidwa ndipo pambuyo pake amulakwiranso, ndithudi, Mulungu adzamuthandiza iye. Ndithudi! Mulungu ndi wachisoni ndiponso wokhululukira.

61. Ichi ndi chifukwa chakuti Mulungu amalowetsa usiku mu usana ndi kulowetsa usana mu usiku. Ndithudi Mulungu ndi wakumva ndi woona.
62. Zonsezi ndi chifukwa chakuti Mulungu ndiye choonadi ndipo zonse zimene iwo amazipembedza kuonjezera pa Mulungu ndi zabodza. Ndithudi Mulungu ndi Wapamwamba ndiponso Wamkulu.

63. Kodi iwe siukuona kuti Mulungu amagwetsa mvula kuchokera kumwamba ndipo kuti nthaka imakhala ndi zomera zobiriwira? Ndithudi Mulungu ndi Mwini chisoni chosatha, wodziwa zonse zobisika ndi zoonekera.
64. Mulungu ndiye mwini zonse za kumwamba ndi dziko lapansi. Ndithudi Mulungu ndi wolemera ndi wotamandidwa.

65. Kodi inu simuona kuti Mulungu wakupeputsirani zonse zimene zili pa dziko lapansi ndi zombo zimene mumayendera pa nyanja ndi chilolezo chake? Iye amagwira thambo kuti lisagwe pansi. Ndithudi Mulungu ndi wachisoni ndiponso wachifundo kwa anthu.
66. Iye ndiye amene adakupatsani moyo ndipo adzapangitsa kuti mufe

ndi kukupatsaninso moyo kachiwiri. Ndithudi munthu ndi
wosathokoza.
67. Ku mtundu uliwonse Ife tidalamulira miyambo
ya chipembedzo imene iwo ayenera kuitsatira ndipo
iwo asakangane ndi iwe pa nkhani iyi. Koma aitanire
kwa Ambuye wako. Ndithudi iwe uli pa njira yoyenera.
68. Ndipo ngati iwo atsutsana ndi iwe, nena "Mulungu
amadziwa bwino zonse zimene inu mumachita."
69. Mulungu adzaweruza, pakati panu, patsiku lachiweruzo,
zimene inu munali kusiyana. 70. Kodi iwe siudziwa kuti
Mulungu amadziwa zonse zimene zili kumwamba ndi pa
dziko lapansi? Ndithudi zonse zidalembedwa m'Buku lake.
Ndithudi zimenezo ndi zosavuta kwa Mulungu.
71. Ndipo iwo ali kupembedza zinthu zina mowonjezera
pa Mulungu, zinthu zimene sanapatsidwe umboni kuti
azizigwadira ndipo ndi zimene iwo salikuzindikira.
Ndithudi, anthu ochimwa alibe wowathandiza. 72. Ndipo
pamene chivumbulutso chathu chomveka chilakatulidwa
kwa iwo, iwe udzaona kukana pa maso pa anthu
osakhulupirira! Iwo ali pafupifupi kumenyana ndi iwo
amene amalakatula chivumbulutso chathu kwa iwo. Nena
"Kodi mufuna ndikuuzeni zoipa kuposa chizindikiro
choterechi? Chizindikirocho ndi moto wa ku Gahena
umene Mulungu walonjeza anthu osakhulupirira ndipo
amenewa ndi malo oipa kupitako."
73. Oh anthu inu! Fanizo laperekedwa ndipo limvetsetseni.
Ndithudi! Iwo amene mumawapembedza kuonjezera
pa Mulungu weniweni sangathe kulenga ntchentche
imodzi ngakhale onse atagwirizana kuti achite choncho.
Ndipo ngati ntchentche italanda kalikonse kuchokera

kwa iwo, iwo sangathe kuilanda ayi. Anthu opempha ndi wopemphedwa onse alibe mphamvu. 74. Iwo sapereka ulemu kwa Mulungu umene uyenera kuperekedwa kwa Iye. Ndithudi Mulungu ali ndi mphamvu ndipo ndi Mwini mphamvu zonse.

75. Mulungu amasankha Atumwi ake pakati pa Angelo ndi pakati pa anthu. Ndithudi Mulungu amamva zonse ndiponso amaona chilichonse. 76. Iye amadziwa zonse zimene zili patsogolo pawo ndi zimene zili m'mbuyo mwawo. Kwa Mulungu zinthu zonse zimabwerera.

77. Oh inu anthu amene mwakhulupirira! Weramani ndipo gunditsani mphumi zanu pansi ndi kupembedza Ambuye wanu ndipo chitani ntchito zabwino kuti mupambane. 78. Ndipo limbikani kwambiri chifukwa cha chipembedzo cha Mulungu monga mmene zikufunikira. Iye wakusankhani inu ndipo sadakukundikireni mavuto muchipembedzo chanu. Chipembedzo cha Abrahamu atate wanu. Iye ndiye amene akupatsani inu dzina lakuti Asilamu kuyambira kalekale ndiponso mu dzinali Mtumwi ndiye mboni yanu, ndipo nanunso mukhale mboni ya anthu anzanu. Pitirizani mapemphero, perekani msonkho wothandizira anthu osauka ndipo khulupiririrani mwa Mulungu. Iye ndi Mtetezi wanu wabwino ndiponso Mthandizi wabwino kwambiri.

# AL-MU-MINUN

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Anthu okhulupirira ndiwo opambana. 2. Iwo amene
amadzichepetsa akamapemphera. 3. Ndi iwo amene
amalewa nkhani zabodza, 4. Ndipo amapereka zaulere
kwa anthu osauka, 5. Ndi iwo amene amadziteteza ku
chiwerewere, 6. Kupatula kwa akazi awo kapena akapolo
awo akazi, chifukwa iwo sangadzudzulidwe. 7. Koma amene
angafune zina pamwamba pa zimene tawaloleza anthu
otere ndi ochimwa; 8. Amene amakwaniritsa malonjezo ndi
mapangano awo, 9. Ndi iwo amene amasunga mapemphero
awo; 10. Amenewa ndithudi ndiwo amene adzalowa, 11. Iwo
adzalowa ku Paradiso ya pamwamba ndipo adzakhalamo
mpaka kalekale.

12. Ndithudi Ife tidapanga munthu kuchokera ku dothi
labwino, 13. Titatero tidamukonza iye kukhala dontho
la umuna m'malo otetezedwa mu msana, 14. Dontho la
umunali tidalipanga kukhala dontho la magazi ndipo
dontho lamagazili tidalipanga kukhala m'bulu wa mnofu.
Ndipo mnofu umenewu tidaukonza kukhala mafupa
ndipo tidakuta mafupa ndi mnofu. Kotero tidamupanga
iye kukhala chilengedwe china. Odalitsa akhale
Mulungu, Namalenga wabwino kwambiri mwa onse.
15. Ndipo pambuyo pake inu nonse mudzafa. 16. Ndipo
mudzapatsidwanso moyo patsiku la kuuka kwa akufa.

17. Ife tidalenga miyamba isanu ndi iwiri pamwamba
panu ndipo kwa zolengedwa zathu. Ndipo Ife sitikhala
osalabadira ayi. 18. Ife timatumiza madzi kuchokera
kumwamba m’muyeso wokwana ndipo timawalowetsa
pansi pa nthaka. Ndipo Ife tili ndi mphamvu yowachotsa
madziwo. 19. Ndipo Ife timakutulutsirani mmenemo
minda ya tende ndi mphesa, m’mene muli zipatso zanu
zambiri zimene zina mwa izo mumadya. 20. Mtengo umene
umamera pa phiri la Sinai, umapereka mafuta ndiponso
ndiwo kwa anthu. 21. M’nyama namonso muli chizindikiro
choonetsa mphamvu zathu. Inu timakumwetsani zimene
zili m’mimba mwake ndipo mumadya nyama yake ndiponso
mumapeza phindu lambiri. 22. Ndipo pa izo ndi m’zombo
zimene zimayenda pa nyanja, inu mumanyamulidwa.

23. Tidamutumiza Nowa kwa anthu ake ndipo iye adati,
“Tumikirani Mulungu anthu anga chifukwa mulibe
mulungu wina koma Iye yekha. Kodi simungamuope Iye?”
24. Akuluakulu osakhulupirira a anthu ake adati, “Munthu
uyu ndi wolingana ndi inu, iye ali kungodziyenereza
kuti ndi wopambana pakati panu.” Mulungu akadafuna,
akadatumiza angelo. Ndiponso zinthu za mtundu uwu
sitidamvepo kuchokera kwa makolo athu akalekale.
25. Ndithudi ameneyu ndi wopenga, ndipo mumuyang’anire
pa kanthawi.”

26. Iye adati, “Ambuye! Ndithandizeni ine chifukwa iwo
ali kundikana.” 27. Ife tidavumbulutsa chifuniro chathu
kwa iye ponena kuti, “Khoma chombo chimene Ife
tidzayang’anira molingana ndi chilangizo chathu. Pamene
chiweruzo chathu chidza ndipo madzi asefukira kuchokera
ku ng’anjo, utenge zolengedwa ziwiriziwiri, zazimuna ndi

zazikazi ndiponso kuchokera kwa iwo a m'nyumba mwako
kupatula okhawo amene adanenedwa kuti adzaonongeka.
Usandipemphe kuti ndipulumutse iwo amene adachita
zoipa chifukwa iwo adzamizidwa."
28. Ndipo pamene iwe ndi iwo amene akutsata iwe mulowa
m'chombo, nena, "Kuyamikidwa kukhale kwa Mulungu
amene watipulumutsa ife kuchoka ku mtundu wa anthu
oipa." 29. Ndipo nena: "Ambuye wanga! Ndithandizeni kuti
ndikafike pamalo podalitsika chifukwa Inu ndinu wabwino
wa onse amene amafikitsa pamalo okocheza." 30. Ndithudi
mu zimenezi muli zizindikiro zooneka. Ndithudi Ife
timawaika anthu m'mayesero.
31. Potero Ife tidapanga mtundu wa anthu a tsopano
pambuyo pawo. 32. Ndipo tidatumiza kwa iwo Mtumwi
wa mtundu wawo amene adati, "Tumikirani Mulungu
chifukwa inu mulibe mulungu wina koma Iye yekha. Kodi
simungamuope Mulungu?" 33. Koma akuluakulu a anthu
osakhulupirira a anthu ake, amene adakana za moyo
umene uli nkudza ndi amene tidawapatsa zinthu zabwino
za m'moyo uno adati, "Munthu uyu ndi munthu monga inu
nomwe amene akudya zimene mumadya inu ndi kumwa
zimene inu mumamwa." 34. "Ngati inu mumvera munthu
wonga inu nomwe, ndithudi, inu mudzatayika."
35. "Kodi iye ali kukuopsezani kuti pamene inu mutafa
ndi kusanduka dothi ndi mafupa mudzadzuka ndi
kukhalanso ndi moyo?" 36. "Zimene inu muli kuopsezedwa
nazo zili kutali." 37. "Kulibenso moyo wina koma moyo
wathu wapadziko lapansi basi. Ife timafa ndi kukhala ndi
moyo ndipo ife sitidzadzukanso ayi." 38. "Munthu uyu ndi

odziyenereza amene ali kunena za Mulungu zimene sizili
zoona ayi. Ife sitidzamukhulupirira.”
39. Iye adati, “Ambuye! Ndithandizeni ine chifukwa
iwo ali kunditsutsa.” 40. Iye adati, “Posachedwapa
iwo adzanong’oneza bombono.” 41. Chilango chathu
chidawapeza mwachilungamo ndipo tidawafafaniza monga
zinyalala. Chionongeko kwa anthu onse ochimwa.
42. Atapita awa tidalenganso mitundu ina ya anthu.
43. Palibe anthu amene angafulumizitse kapena kuchedwetsa
chionongeko chawo. 44. Ndipo Ife tidatumiza Atumwi
ena motsagana ndipo nthawi iliyonse Mtumwi amadza
kwa iwo ndipo amamukana nati ndi wabodza. Ndipo Ife
tidawaononga ena pambuyo pawo ndipo tidawapanga iwo
kukhala chitsanzo cha mbiri ya anthu olakwa. Ichi chidali
chionongeko cha anthu osakhulupirira.
45. Ndipo Ife tidamutumiza Mose pamodzi ndi m’bale
wake Aroni ndi zizindikiro ndiponso ulamuliro wathu.
46. Kwa Farawo ndi nduna zake ndipo iwo adawalandira
mwamwano chifukwa iwo adali anthu a chipongwe.
47. Ndipo iwo adati, “Kodi ife tikhulupirire anthu awiri
olingana ndi ife amene anthu awo ndi akapolo athu?”
48. Iwo adawakana iwo kotero iwo adalandira chionongeko.
49. Ndipo Ife tidamupatsa Mose Buku la Chipangano
Chakale kuti anthu ake akhoza kutsogozedwa bwino.
50. Ife tidamupanga mwana wamwamuna wa Maria
pamodzi ndi amayi ake kukhala chizindikiro kwa anthu
onse ndipo tidawapatsa mnthunzi pa malo okwera ndi
malo a mtendere amene anali kuthiriridwa ndi madzi a pa
kasupe.
51. Oh Atumwi! Idyani zinthu zabwino ndipo muzichita

ntchito zabwino. Ndithudi Ine ndimadziwa zonse zimene
mumachita. 52. Ndithudi chipembedzo chanu ndi chimodzi
ndipo Ine ndine Ambuye wanu. Kotero ndiopeni Ine.
53. Koma anthu adagawanika m'magulu osiyanasiyana,
gulu lililonse limasangalala ndi ziphunzitso zawo.
54. Alekeni ayambe achimwa mpaka pamene imfa iwapeza.
55. Kodi iwo amaganiza kuti popeza tawapatsa chuma ndi
ana. 56. Ndiye kuti Ife tili kuwafunira zabwino? Iyayi. Iwo
sadziwa kanthu ayi.
57. Ndithudi iwo ndi anthu amene amaopa Ambuye
wawo. 58. Amene amakhulupirira zizindikiro za Ambuye
wawo. 59. Amene sapembedza wina aliyense poonjezera pa
Ambuye wawo. 60. Amene amapereka chaulere mitima ili
yoopa Ambuye wawo chifukwa chakuti adzabwerera kwa
Iye. 61. Awa ndiwo amene amapikisana wina ndi mnzake
pochita zabwino ndipo amakhala oyamba pozindikira.
62. Ife sitinyamulitsa mzimu wina uliwonse katundu amene
iwo sangathe kunyamula. M'buku lathu mudalembedwa
zoona zokhazokha. Ndipo palibe munthu amene
adzaponderezedwa.
63. Koma mitima ya anthu osakhulupirira siyizidziwa
zimenezi ayi. Iwo ali ndi ntchito zina zoipa kupatula
zimene iwo amachita. 64. Koma pamene chilango chathu
chidza pa iwo amene amakhala mu mtendere, iwo adzafuula
kufuna chithandizo. 65. Musalire tsiku la lero chifukwa inu
simudzalandira chithandizo china chilichonse kuchokera
kwa Ife. 66. Chivumbulutso changa chinali kulakatulidwa
kwa inu nthawi zambiri koma inu munali kuthawa ndi
kuchikana mwamwano. 67. Inu mumachinyoza usana ndi
usiku uliwonse.

68. Kodi iwo sangathe kulingalira mozama
pa mawu a Mulungu kapena pali china chake
chimene chidavumbulutsidwa kwa iwo chimene
sichidavumbulutsidwe kwa makolo awo? 69. Kapena iwo
sadziwa kuti akukana Mtumwi wawo? 70. Kapena iwo akuti
Iye ndi wopenga? Koma iye wawabweretsera iwo onse
zoonadi. Koma ambiri amakana choonadi. 71. Kukadakhala
kuti choonadi chimatsatira zofuna zawo, ndithudi,
kumwamba, dziko lapansi ndi onse okhala m’menemo
akadaonongeka. Ife tawapatsa chikumbutso komabe iwo
safuna kumvera chikumbutsocho.

72. Kapena iwe uli kuwapemphera mphotho? Chithandizo
cha Ambuye wawo ndicho chabwino. Ndipo Iye ndiye
wopereka moolowa manja kuposa onse amene amapereka.
73. Ndithudi iwe uli kuwaitana kuti adze kunjira yoyenera.
74. Ndithudi iwo amene amakana moyo umene uli nkudza
adzakhala ali kusochera ku njira yoyenerayi.

75. Ngati Ife tikadawalangiza chisoni chathu ndi
kuwachotsera mavuto, iwo akadakhala ali kulakwabe
m’njira zawo zoipa ndi kusokonezeka ndi zoipazo.
76. Ndithudi tidawalanga kale koma iwo sadafunefune
Ambuye wawo kapena kukhala odzichepetsa pamaso pake.
77. Mpaka pamene tidzawatsekulira khomo la chilango
chowawa, iwo adzakhala okhumudwa.

78. Iye ndiye amene adakupatsani makutu, maso ndi
mitima. Komabe inu simuthokoza mokwanira. 79. Iye ndiye
amene adakulengani ndi kukuchulukitsani padziko lapansi
ndipo nonsenu mudzasonkhanitsidwa kudza pamaso pake.
80. Iye ndiye amene amapereka moyo ndiponso imfa ndipo

ndi Iyenso amene amasithanitsa usiku ndi usana. Kodi
simungazindikire?
81. Iwo amanena zimene anthu akale ankanena. 82. Iwo
amati, “Pamene ife tafa ndi kusanduka dothi ndi mafupa,
kodi tidzadzukanso ndi kukhala ndi moyo?” 83. Ndithudi ife
tidalonjedzedwa zimenezi kale pamodzi ndi makolo athu.
Izi si zina ayi koma nkhani zabodza za anthu a makedzana.
84. Nena, “Kodi Mwini wake wa dziko lapansi ndi zonse
zimene zili mmenemo ndani? Ndiuzeni ngati mumudziwa.”
85. Iwo adzati, “Mwini wake ndi Mulungu.” Nena, “Kodi
inu simungachenjezedwe?” 86. Nena, “Kodi Ambuye wa
miyamba isanu ndi iwiri ndiponso Mwini Ufumu ndani?”
87. Iwo adzati, “Mwini wake ndi Mulungu.” Nena, “Nanga
kodi simungasiye kuchita zoipa?” 88. Nena, “Kodi ulamuliro
wa zinthu zonse zili m’manja mwa yani? Kodi ndani amene
amaziteteza zonse pamene Iye safuna chitetezo cha wina
aliyense ngati inu mukudziwa?” 89. Iwo adzati, “M’manja
mwa Mulungu.” Nena, “Nanga ndi chifukwa chiyani inu
mwanyengedwa?”
90. Iyayi, Ife tawavumbulutsira choonadi. Koma onsewa
ndi anthu abodza. 91. Palibe nthawi imene Mulungu adabala
mwana ndipo kulibe Mulungu wina woonjezera pa Iye.
Ngati izi zikadakhala choncho, bwezi Mulungu aliyense
akumatenga zolengedwa zake zokha ndi kumaziika
pamwamba pa zolengedwa za Mulungu wina. Ulemerero
ukhale kwa Mulungu woposa zina zilizonse! 92. Iye
amadziwa zonse zooneka ndiponso zobisika. Mulungu
akhale wopambana milungu ina imene iwo amaitumikira.
93. Nena, “Ambuye wanga! Ngati Inu mukadandionetsa
chilango chimene muli kuwopseza, 94. Ambuye wanga!

Pulumutsani ndipo musandisiye ine pakati pa mtundu
wa anthu oipawu.” 95. Ndithudi, Ife tili ndi mphamvu zoti
ukhoza kuona chilango chimene tawaopseza.

96. Dzitetezeni ndi chabwino pothamangitsa choipa. Ife
tili kudziwa zonse zimene ali kukunamizirani. 97. Ndipo
iwe unene kuti, “Ambuye wanga, Ine ndili kufuna chitetezo
chanu pothawa zoipa za Satana.” 98. “Ambuye! Ine ndili
kupempha chitetezo chanu kuti asabwere kumene ndili
ine.” 99. Mpaka pamene imfa idza kwa munthu wolakwa
iye adzati, “Ambuye wanga! Bwezeni.” 100. “Kuti ndikachite
ntchito zabwino zimene ndidalephera kuchita.” Kosatheka!
Amenewa ndiwo mawu chabe amene akungolankhula.
Kumbuyo kwawo kudzakhala chipupa mpaka pa tsiku la
kuuka kwa akufa. 101. Ndipo pamene lipenga lidzaombedwa,
pa tsiku limeneli, ubale wawo wonse udzathera pomwepo
ndiponso sadzafunsana chithandizo chochokera kwa wina
ndi mnzake. 102. Aliyense amene muyeso wake udzakhala
wolemera, adzapambana. 103. Koma aliyense amene muyeso
wake udzakhala wopepuka adzataya moyo wake ndipo
adzakhala ku Gahena nthawi zonse. 104. Moto udzatentha
nkhope zawo ndipo izo zidzakwinyikakwinyika chifukwa
chaululu.

105. “Kodi chivumbulutso chathu sichidalakatulidwe
kwa inu? Kodi simudachikane?” 106. Iwo adzati, “Ambuye
wathu! Zilakolako zathu zidatigonjetsa ife ndipo tidali
anthu osochera.” 107. “Ambuye wathu! tipulumutseni ife
ku ichi. Ngati ife tidzabwereranso ku zoipa, ndithudi, ife
tidzakhala anthu oipa kwambiri.” 108. Iye adzati, “Khalani
mu icho mwamanyazi ndipo musandiyankhulitse Ine
ayi.” 109. Ndithudi padali gulu la Atumiki anga amene

adati, "Ambuye wathu! Ife timakhulupirira mwa inu.
Tikhululukireni ndipo mutichitire chisoni. Inu ndinu
wabwino pochita chisoni kuposa a chisoni onse."
110. Koma inu munali kuwanyogodola mpaka pamene
inu mudandiiwala Ine ndipo inu munali kuwaseka iwo.
111. Ndithudi lero Ine ndawalipira chifukwa cha kupirira
kwawo ndipo iwo ndi amene apambana.

112. Ndipo Iye adzafunsa kuti, "Kodi inu munakhala
padziko lapansi zaka zingati?" 113. Iwo adzayankha kuti,
"Takhala tsiku limodzi kapena mphindi zochepa zokha.
Afunseni iwo amene amasunga chiwerengero." 114. Iye
adzawayankha kuti, "Inu mukadadziwa ndi nthawi yochepa
kwambiri imene inu munakhala."

115. "Kodi inu mumaganiza kuti tidangokulengani inu
opanda cholinga ndipo kuti simudzabwerera kwa Ife?"
116. Motero alemekezeke Mulungu, Mfumu ya chilungamo.
Palibe Mulungu wina koma Iye yekha, Ambuye wa
Mpando wolemekezeka ndi Wachifumu. 117. Aliyense
amene apembedza mulungu wina woonjezera pa Mulungu,
pamene Iye alibe umboni wa chimenecho, Ambuye
wake adzamufunsa. Ndithudi anthu osakhulupirira
sadzapambana ayi. 118. Nena, "Ambuye wanga!
Ndikhululukireni machimo anga ndipo mundichitire
chisoni chifukwa Inu ndinu wachisoni choposa a chisoni
onse."

# AL NUR

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ife tavumbulutsa mutu uwu ndipo taupanga kukhala
wokakamiza ndipo ndi mwa iwo mmene tavumbulutsa
chivumbulutso choonekakuti inu mukhoza kuchenjezedwa.
2. Munthu wamkazi wosakwatiwa akachita chigololo ndi
munthu wamwamuna wosakwatira, mukwapule aliyense
wa iwo zikoti zana limodzi ndipo musalole kuti chifundo
chikulepheretseni kumvera lamulo la Mulungu ngati inu
mumakhulupirira mwa Mulungu ndi tsiku lomaliza. Ndipo
onetsetsani kuti chilango chawo chachitidwa umboni
ndi anthu ambiri okhulupirira. 3. Mwamuna wachigololo
asakwatire wina koma mkazi wachigololo kapena mkazi
wopembedza mafano. Mkazi wachigololo asakwatiwe ndi
wina koma mwamuna wachigololo kapena wopembedza
mafano. Anthu okhulupirira moona saloledwa maukwati
otere.

4. Iwo amene amanamizira akazi odzisunga kuti achita
chigololo ndipo sangathe kutulutsa mboni zinayi,
akwapulidwe zikoti makumi asanu ndi atatu. Mukane
umboni wawo mpaka kalekale. Anthu otere ndi oononga.
5. Kupatula okhawo amene, patapita nthawi, alapa ndi kusiya
makhalidwe awo onyansa. Mulungu ndi wokhululukira ndi
Mwini chisoni chosatha.

6. Ndipo ngati mwamuna akuti mkazi wake wachita

chigololo koma alibe mboni kupatula iye mwini, iye
alumbire kanayi dzina la Mulungu kuti zimene ali kunena
ndi zoona. 7. Ndipo kachisanu anene kuti matemberero
a Mulungu akhale pa iye mwamunayo ngati ali kunama.
8. Koma ngati mkazi wake alumbira kanayi, potchula dzina
la Mulungu, kutsutsa kuti zimene ali kunena mwamuna
wake ndi zabodza, sadzalandira chilango. 9. Ndipo
kachisanu ayenera kunena kuti mkwiyo wa Mulungu ukhale
pa iye mkaziyo ngati ali kunama. 10. Pakadapanda chisoni
ndi chisomo cha Mulungu mukadaonongeka. Ndithudi
Mulungu ndi wokhululukira ndi waluntha.

11. Iwo amene adapeka nkhani yabodzayi, adali gulu la
anthu anu omwe. Usaganize kuti ndi masoka koma ndi
zabwino kwa inu. Aliyense adzalangidwa molingana ndi
tchimo lake. Akakhala iye amene amaikulitsa nkhaniyi,
chilango chake chidzakhala chowawa kwambiri.

12. Pamene mudamva nkhaniyi, bwanji anthu okhulupirira,
amuna ndi akazi, sadafune kuganizira zabwino za anthu
awo ndi kunena kuti, "Ili ndi bodza loonekera poyera?"
13. Kodi ndi chifukwa chiyani iwo sadabweretse mboni
zinayi? Ngati iwo adalephera kutulutsa mboni ndiye kuti
iwo anali kunama pamaso pa Mulungu.

14. Kukadakhala kuti Mulungu sadaonetse chisomo ndi
chifundo chake pa inu, m'moyo uno ndiponso m'moyo
umene uli nkudza, mukadalangidwa kwambiri chifukwa
cha zimene mwakhala mukuchita. 15. Pamene inu munali
kunena ndi malirime anu ndiponso kuyankhula ndi
pakamwa panu zinthu zimene simunali kuzidziwa, inu
munali kuganiza kuti izi zidali zopepuka koma pamaso pa
Mulungu zinali zazikulu. 16. Pamene mudazimva, bwanji

inu simudanene kuti, “Si koyenera kuti ife tikambe izi
ayi. Mulungu ayeretsedwe! Kumeneku ndiko kunama
kwenikweni.” 17. Mulungu ali kukuchenjezani kuti
musadzachitenso izi ngati inu ndinu anthu okhulupirira
m’choonadi. 18. Mulungu ali kukufotokozerani momveka
chivumbulutso chake. Iye ndi wanzeru ndipo amadziwa
zonse.

19. Iwo amene amasangalala kuti nkhani zoipa zokhudza
anthu okhulupirira zifalikire, adzalangidwa kwambiri
m’moyo umene uli nkudza. Mulungu ali kudziwa zonse
pamene inu simudziwa. 20. Pakadakhala popanda chisomo
cha Mulungu kwa inu, nonse mukanaonongedwa.
Ndithudi Mulungu ndi wabwino ndiponso wachisoni.
21. Oh inu anthu okhulupirira m’choonadi! Musatsatire
mapazi a Satana. Aliyense amene atsatira mapazi a Satana,
ndithudi, iye amalamulira zinthu zochititsa manyazi
ndi zoipa. Koma pakadapanda chisomo cha Mulungu,
panalibe wina wa inu amene akadayeretsedwa zoipa zake.
Koma Mulungu amayeretsa aliyense amene Iye wamufuna.
Mulungu amamva zonse ndiponso amadziwa chinthu china
chilichonse.

22. Musalole kuti anthu olemera ndi olemekezeka amene
ali pakati panu kuti alumbire kuti sadzapereka chithandizo
kwa abale awo, kwa anthu osauka ndiponso kwa iwo amene
adathawa ku midzi yawo chifukwa cha nkhani zokhudza
Mulungu. Iwo ayenera kuwakhululukira ndi kuwalekerera.
Kodi inu simufuna kuti Mulungu akukhululukireni?
Mulungu ndi Mwini chikhululukiro ndiponso Mwini
chisoni chosatha.

23. Onse amene amaipitsa mbiri ya akazi odzisunga

ndiponso okhulupirira amene sachita zoipa, adzakhala
otembereredwa m'dziko lino ndiponso mulimene lili
nkudza. Chawo chidzakhala chilango choopsa. 24. Patsikuli
malirime awo, manja awo, ndi miyendo yawo zidzachitira
umboni pa zimene iwo anali kuchita. 25. Patsiku limeneli
Mulungu adzawapatsa dipo lawo loyenera, ndipo iwo
adzadziwa kuti Mulungu ndiye choonadi chenicheni.
26. Zinthu zodetsedwa ndi zoyenera anthu odetsedwa
ndipo zinthu zosadetsedwa ndi za anthu osadetsedwa,
ndiponso zinthu zabwino ndi zoyenera anthu abwino.
Kotero anthu abwino ndi oyenera zinthu zabwino
ndipo anthu otere sakhudzidwa ndi zimene akunena;
iwowa adzakhululukidwa ndipo adzapatsidwa mphotho
yolemekezeka.
27. Oh inu anthu okhulupirira! Musalowe m'nyumba za
anthu ena pokhapokha mutapempha chilolezo cha eni
ake ndipo alonjereni powafunira iwo mtendere. Zimenezo
ndi zabwino kwa inu kuti muchenjezedwe. 28. Mukapeza
kuti kulibe aliyense, musalowe mpaka pokhapokha
mwapatsidwa chilolezo. Ngati akuuzani kuti mubwerere
kapena musalowe, ndi chilungamo kuti inu mubwerere
kupita komwe mwachokera. Zimenezo ndi zabwino
kwa inu. Mulungu amadziwa zonse zimene mumachita.
29. Sichidzakhala cholakwa ngati inu mulowa m'nyumba
zopanda okhalamo zomwe muli nazo ndi ntchito. Mulungu
amadziwa zonse zimene mumaulula ndi zimene mumabista.
30. Auze amuna okhulupirira kuti azitsitsa maso awo ndi
kulewa chigololo. Zimenezi ndizo zimene zidzayeretsa
moyo wawo. Mulungu amadziwa zonse zimene mumachita.
31. Auze akazi okhulupirira kuti azitsitsa maso awo ndipo

asachite chiwerewere ndiponso azibisa zinthu zimene zimawakongoletsa kupatula zokhazo zimene sizingabisike. Ndipo azifunda nsalu kumutu ndi pa chifuwa chawo ndiponso asaonetse kukongola kwawo kupatula kwa amuna awo, abambo awo, abambo a amuna awo, ana awo aamuna, ana a amuna awo, ana a chemwali awo kapena ana a achimwene awo kapena ana a alongo awo kapena akazi anzawo owakhulupirira; ndiponso antchito awo aakazi, a ntchito awo a amuna ndi ana amene alibe chilakolako cha akazi. Ndipo iwo asamamenyetse mapazi awo pansi akamayenda ndi cholinga choonetsa zina zokongola zawo zobisika. Oh inu okhulupirira! Lapani kwa Mulungu mogonja kuti mupambane.

32. Kwatiranani ndi iwo a pakati panu amene ndi osakwatiwa ndiponso akapolo anu aamuna kapena aakazi amene ali olungama. Ngati iwo ndi osauka, Mulungu adzawalemeretsa iwo kuchokera ku zabwino zake. Mulungu ndiye wopatsa ndi wodziwa. 33. Onse amene sangathe kukwatira adzisunge mpaka pamene Mulungu awapatsa iwo zabwino zake. Akakhala a kapolo anu amene afuna kugula ufulu wawo, amasuleni ngati inu muona kuti iwo ndi abwino ndipo muwapatseko gawo la chuma chimene Mulungu wakupatsani inu. Inu musadzakakamize akapolo anu aakazi kuti azichita chiwerewere ngati iwo afuna kudzisunga ndi cholinga chofuna kupeza zinthu zabwino za padziko lapansi. Ngati wina aliyense awakakamiza iwo, Mulungu adzawakhululukira ndi kuonetsa chisoni chake pa iwo. 34. Ife takutumizirani inu chivumbulutso chooneka bwino ndipo takupatsani chitsanzo cha anthu amene adalipo kale ndi chilangizo kwa anthu angwiro.

35. Mulungu ndi Muuni wa kumwamba ndi dziko lapansi.
Kuunika kwake kukhoza kufaniziridwa ndi malo olowa
m'chipupa amene m'kati mwake muli nyali imene ili
m'galasi looneka ngati nyenyezi yowala. Iyo imayatsidwa
kuchokera ku mtengo wodalitsika wa Azitona umene
siuli kum'mawa kapena kumadzulo. Mafuta ake amatha
kuwala ngakhale kuti palibe moto owayakitsa mafutawo.
Muuni pa Muuni unzake ndipo Mulungu amatsogolera, ndi
kuwala kwake, aliyense amene Iye wamufuna. Mulungu
amapereka zitsanzo kwa anthu. Ndipo Mulungu amadziwa
chilichonse.
36. M'nyumba zimene Mulungu adalamula kuti
zimangidwe ndipo m'menemo dzina lake limakumbukirika,
Mulungu amalemekezeka m'menemo m'mawa ndi
madzulo. 37. Pali anthu amene malonda kapena zogulitsa
sizingathe kuwaiwalitsa kukumbukira Mulungu kapena
kupemphera kapena kupereka msonkho wothandiza
anthu osauka. Iwo amene amaopa tsiku limene mitima ndi
maso adzatembenuka. 38. Kotero Mulungu adzawalipira
chifukwa cha ntchito zawo zabwino ndiponso adzawapatsa
zabwino zochokera m'chisomo chake. Mulungu amapereka
mopanda muyeso kwa aliyense amene Iye wamufuna.
39. Akakhala anthu osakhulupirira, ntchito zawo zili ngati
chizirezire cha m'chipululu. Wapaulendo amene ali ndi
ludzu amaganiza kuti ndi madzi koma akachiyandikira
amaona kuti palibe chilichonse. Iye amamupeza Mulungu
pomwepo amene amamupatsa molingana ndi ntchito zake.
Mulungu amachita chiwerengero cha zinthu mofulumira.
40. Kapena monga mdima wa m'nyanja yozama kwambiri
yokutidwa ndi mafunde aakulu oyenda pamwamba pa

mafunde anzake ndi mitambo pamwamba pake ndiponso
mdima wosanjana ndi mdima unzake. Ndipo ngati iye
atambasula dzanja lake sangathe kuliona. Ndithudi
munthu amene saunikidwa ndi Mulungu sangathe kuona
kuwala kwa mtundu wina uliwonse.
41. Kodi iwe siunaone kuti zonse zimene zili kumwamba
ndi pa dziko la pansi zimalemekeza Mulungu ndiponso
pamene mbalame zikutambasula mapiko ake? Chilichonse
chimadziwa mapemphero ndi mayamiko omupatsa Iye
ndipo Mulungu amadziwa ntchito zawo zonse. 42. Ndipo
Mulungu ndiye mwini ufumu wa kumwamba ndi wa
padziko lapansi. Ndi kwa Mulungu kumene zinthu zonse
zidzabwerera.
43. Kodi inu simuona mmene Mulungu amayendetsera
mitambo? Ndipo amaisonkhanitsira ndi kuiika m'gulu
limodzi ndipo inu mumaona mvula ili kuchokera mu
mitamboyo. Kuchokera ku mapiri a kumwamba, Iye
amatumiza mphepo kuti ipeze kumupeza wina aliyense
amene wamufuna ndi kusiya aliyense amene wamufuna.
Chilangali cha mphenzi zake chimakhala pang'ono kuti
chilande maso a anthu. 44. Mulungu amasanduliza usiku
ndi usana. Ndithudi mu izi muli chizindikiro kwa anthu
ozindikira.
45. Mulungu adalenga cholengedwa chilichonse
kuchokera ku madzi ndipo zina zimayenda chafufumimba,
zina zimayenda ndi miyendo iwiri ndi zina zimayenda ndi
miyendo inayi. Mulungu amalenga chilichonse chimene
wafuna. Ndithudi Mulungu ali ndi mphamvu pa chinthu
china chilichonse. 46. Ndithudi Ife tatumiza chivumbulutso

choonetsa choonadi. Ndipo Mulungu amalangiza aliyense
amene Iye wamufuna ku njira yoyenera.
47. Iwo amanena monenetsa kuti, "Ife timakhulupirira
mwa Mulungu ndi Mtumwi wake ndipo timawamvera
onsewa." Koma pambuyo pake ena a iwo amabwerera
m'mbuyo. Ndithudi awa si okhulupirira ayi. 48. Ndipo
pamene iwo amaitanidwa kuti adze kwa Mulungu ndi
Mtumwi wake, kuti akhoza kuwaweruza, ena amakana.
49. Chikadakhala kuti choonadi chili mwa iwo, iwo akadadza
kwa iye modzipereka. 50. Kodi m'mitima mwawo muli
matenda kapena ali ndi chikayiko? Kapena iwo amaopa
kuti Mulungu ndi Mtumwi wake akhoza kuwakaniza
chiweruzo cholungama? Koma oterewa ndi ochita zoipa.
51. Koma pamene anthu okhulupirira enieni amaitanidwa
kwa Mulungu ndi Mtumwi wake kuti akhoza kuwaweruza,
yankho lawo limangokhala lakuti, "Tamva ndipo titsatira."
Anthu otere ndiwo opambana. 52. Ndipo iye amene amvera
Mulungu ndi Mtumwi wake ndi kuopa Mulungu ndipo
amadzichepetsa kwa Iye, oterewa ndi opambana.
53. Iwo amalumbira pali Mulungu molimba kuti ngati iwe
uwalamulira kumenya nkhondo, adzakumvera iwe. Nena
"Musalumbire ayi! Chofunika ndi kumvera basi. Ndithudi
Mulungu amadziwa chilichonse chimene mumachita."
54. Nena "Mverani Mulungu ndipo mverani Mtumwi wake.
Ngati simungamvere, iye ali ndi udindo wake monga
momwe inu muli ndi udindo wanu. Ngati inu mumumvera,
inu mudzatsogozedwa ndipo udindo wa Mtumwi ndi
kungopereka uthenga womveka."
55. Mulungu walonjeza ena a inu amene akhulupirira ndipo
amachita ntchito zabwino kuti adzawasandutsa kukhala

olowa m'malo padziko monga momwe adasandutsira anthu amene adalipo kale iwo asanadze. Ndipo Iye adzawapatsa mphamvu yoyendetsa chipembedzo chawo chimene adawasankhira. Ndithudi Iye adzawapatsa m'malo mwake chitetezo chokwana atawachokera mantha ngati iwo andipembedza Ine ndipo sandiphatikiza ndi china chilichonse. Ndipo onse amene sakhulupirira atamva izi ndi ochimwa.

56. Kwaniritsani mapemphero anu, perekani msonkho wothandiza osauka, ndipo muzimvera Mtumwi kuti mupeze chisomo cha Mulungu. 57. Musaganize kuti anthu osakhulupirira adzathawa mdziko lino. Moto ndi imene idzakhala mudzi wawo. Ndipo kutsiliza koipa.

58. Oh inu anthu okhulupirira! Lolani akapolo anu aamuna ndi aakazi ndi ana amene sanathe msinkhu kuti apemphe poyamba pa nthawi zitatu, musadapemphere pemphero la m'mawa kapena pamene mwavula zovala zanu masana chifukwa cha kutentha kapena mutatha kupemphera mapemphero a usiku. Izi ndi nthawi zitatu zokhala panokha. Palibe chifukwa kwa inu kapena kwa iwo kuchezerana, wina ndi mnzake mu nthawi zina kupatula nthawi zimene zatchulidwazi. Kotero Mulungu amaulula poyera chivumbulutso chake kwa inu. Ndipo Mulungu ndi Wodziwa ndi Waluntha. 59. Ndipo pamene ana akula msinkhu, alekeni kuti apemphe chilolezo chanu monga akuluakulu awo amachitira. Kotero ndi mmene Mulungu amaululira chivumbulutso chake kwa inu. Ndipo Mulungu ndi wodziwa ndi waluntha. 60. Sichidzakhala cholakwa kwa amayi okalamba amene alibe maganizo a ukwati ngati angasiye zovala zawo zakunja popanda kuonetsa

kukongola kwawo. Kungakhale bwino ngati iwo angavale modzilemekeza. Ndipo Mulungu ndi wakumva ndi wodziwa.

61. Si cholakwa ngati munthu wakhungu kapena wolumala kapena wodwala kapena inu eni ake mudya m'nyumba zanu kapena m'nyumba za atate anu kapena m'nyumba za amayi anu kapena m'nyumba za achimwene anu kapena m'nyumba za alongo anu kapena m'nyumba za achimwene a atate anu kapena alongo awo atate anu kapena m'nyumba za amalume anu kapena m'nyumba za achemwali a amayi anu kapena m'nyumba zimene makiyi ake mwasunga kapena aliyense m'nyumba za abwenzi anu. Palibe cholakwa kwa inu ngati mudya pamodzi kapena payekha payekha. Pamene mulowa m'nyumba, lonjeranani wina ndi mnzake malonje odalitsika ochokera kwa Mulungu. Kotero Mulungu ali kukufotokozerani zizindikiro kuti mukhoza kukhala ozindikira.

62. Ndi okhawo amene ali ndi chikhulupiriro, amene amakhulupirira mwa Mulungu ndi Mtumwi wake ndipo amati akasonkhana pamodzi ndi iye pa zinthu zofunika sachoka mpaka pamene apempha chilolezo chake. Ndithudi anthu amene amakupempha chilolezo ndiwo amene amakhulupirira mwa Mulungu ndi Mtumwi wake. Pamene akupempha iwe chilolezo choti achoke ndi cholinga chokagwira ntchito zawo, pereka chilolezo kwa aliyense amene iwe wamufuna ndipo mumupemphe Mulungu kuti awakhululukire machimo awo. Mulungu amakhululukira ndipo ndi wachisoni chosatha.

63. Musamuitane Mtumwi pomutchula dzina monga momwe mumaitanirana wina ndi mnzake. Mulungu

amadziwa ena a inu amene amazemba ndi kuchoka pakati
panu. Aleke onse amene samvera Mtumwi kuti achenjere
mwina mayesero kapena chilango chowawa chikhoza
kugwa pa iwo. 64. Ndithudi mwini wake wa chilichonse
chimene chili kumwamba ndi dziko lapansi ndi Mulungu.
Ndithudi Iye amadziwa zonse zimene zili m'mitima
mwanu. Ndipo patsiku limene iwo adzabwerera kwa Iye,
Iye adzawauza zonse zimene amachita. Ndipo Mulungu
amadziwa chinthu china chilichonse.

Sura 25 • Al-Fur‘kân

# Al Furqan

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha.

1. Alemekezeke Iye amene adavumbulutsa Korani kwa
Mtumwi wake kuti akhoza kuchenjeza mitundu ya anthu.
2. Iye ndiye Mfumu ya kumwamba ndi dziko lapansi. Iye
ndiye amene sadabereke mwana ndipo alibe wothandizana
naye mu Ufumu wake. Iye ndiye amene adalenga zinthu
zonse ndipo adakhazikitsa mmene zili ndi mapeto ake.
3. Komabe anthu osakhulupirira amapembedza milungu ina
yoonjezera pa Mulungu weniweni imene siingathe kulenga
china chilichonse chifukwa chakuti nayonso idachita
kulengedwa. Ndi imene singathe kuwathandiza kapena
kuwaononga ndiponso imene ilibe mphamvu pa nkhani
zokhudza imfa kapena moyo kapena kuukitsa anthu akufa.
4. Anthu osakhulupirira amanena kuti, "Zonsezi ndi

zinthu zabodza zimene wapeka yekha, ndiponso anthu ena
amamuthandiza. Zonse zimene watulutsa ndi zopanda pake
ndipo zabodza. 5. Ndipo iwo amati, "Izi ndi nkhani zopanda
pake za anthu amakedzana zimene iye walemba. Izo
zimalembetsedwa kwa Iye m'mawa ndi masana aliwonse."
6. Nena, "Wavumbulutsa ndiye amene amadziwa zinsinsi
za kumwamba ndi za padziko lapansi. Iye amakhululukira
ndipo ndi Mwini chisoni chosatha."
7. Iwo amanena kuti, "Uyu, ndi Mtumwi wotani amene
amadya ndipo amayendayenda ku msika? Kodi bwanji
mngelo sanathe kutumizidwa pansi pamodzi ndi iye
kudzatichenjeza ife?" 8. "Nanga ndi chifukwa chiyani
sadapatsidwe chuma ndipo alibe munda woti azipezako
chakudya?" Ndipo anthu ochita zoipa amati, "Ndithudi
munthu amene muli kumutsatira ndi wolodzedwa."
9. Taona mafanizo amene amakupatsa iwe! Iwo asochera
ndipo sangathe kubwerera kunjira yoyenera.
10. Alemekezeke Iye amene, ngati afuna akhoza
kukupatsa iwe zinthu zabwino kuposa zimenezi monga
minda yothiriridwa ndi madzi a m'mitsinje ndi nyumba
zachifumu. 11. Iyayi. Iwo amakana ola lachiweruzo,
ndipo iwo amene amakana olali, Ife tawakonzera moto
woyaka. 12. Pamene idzawaona iwo kuchokera kutali, iwo
adzamva mkokomo wake. 13. Ndipo onse akadzamangidwa
limodzi, adzaponyedwa kumalo opanikizika. Ndithudi
iwo adzafuna imfa itadza pa iwo. 14. Lero musaitane imfa
imodzi yokha ayi koma itanani imfa zambiri. 15. Nena, "Kodi
chimenecho ndi chabwino kapena Paradiso yosatha imene
anthu angwiro adalonjezedwa?" Imeneyo ndiyo mphotho
yawo ndi kobwerera kwawo. 16. Iwo adzapeza m'menemo

zonse zimene anali kufuna ndi kukhala momwemo.
Limenelo ndilo lonjezo limene ndi lofunika kumapempha
pafupipafupi kuchokera kwa Ambuye wako.
17. Patsiku limene Iye adzawasonkhanitsa onse ndi zomwe
amapembedza kuonjezera pa Mulungu weniweni ndipo
Iye adzati, “Kodi ndinu amene munasocheza akapolo anga
kapena ndi iwo okha anasochera ku njira yoyenera?” 18. Iwo
adzati, “Ulemerero ukhale kwa Inu! Si koyenera kwa ife
kuti tisankhe otisamalira ena oonjezera pa Inu. Koma Inu
mudawapatsa iwo ndi makolo awo zinthu zokoma za dziko,
kotero kuti iwo adaiwala chenjezo lanu ndipo adali anthu
oonongeka.” 19. Kotero iwo adatsutsa mawu anu ndipo
inu simungathe kuthawa kapena kupeza chithandizo
ndipo aliyense amene ndi wosalungama pakati panu, Ife
tidzamupatsa chilango chachikulu.
20. Ife sitidatumizepo Atumwi kale amene sanali kudya
ndi kuyenda m’misika. Ife tidakupangani ena a inu kukhala
mayesero a ena. Kodi simungapirire? Ambuye wanu
amaona chilichonse.
21. Iwo amene alibe chikhulupiriro choti adzakumana
ndi Ife amati, “Kodi ndi chifukwa chiyani angelo
sadatumizidwe kwa ife? Kapena ndi chifukwa chiyani kuti
ife sitingaone Ambuye wathu?” Ndithudi iwo adadzikweza
kwambiri. 22. Patsiku limene iwo adzaona angelo, anthu
ochita zoipa sadzasangalala ayi ndipo iwo adzati, “Ambuye
wathu! Ikani malire pakati pa ife ndi iwo.” 23. Ndipo Ife
tidzabweretsa zonse zimene adachita ndikuzionetsa kuti
ndi zinthu zopanda ntchito ngati fumbi louluka. 24. Anthu
okhala ku Paradiso, adzakhala kumalo abwino patsiku
limeneli ndiponso malo abwino opumulako.

25. Patsiku limeneli kumwamba pamodzi ndi mitambo
yake idzagawanika pakati ndipo angelo adzatumizidwa
pansi pano m'maudindo awo. 26. Patsiku limeneli ufumu
wonse udzakhala wa Mwini chisoni chosatha. Limeneli
lidzakhala tsiku lovuta kwambiri kwa anthu osakhulupirira.
27. Patsiku limeneli munthu ochita zoipa adzanong'oneza
bombono nati, "Oh zikadakhala bwino ndikadakhala
kuti ndidatsatira zimene Mtumwi anali kunena!" 28. "Oh
kalanga ine! Ndikadakhala kuti sindidasankhe a uje ndi
a uje kuti akhale anzanga!" 29. "Mosakayika ndiwo amene
adandisokoneza ine kuti ndisakhulupirire machenjezo a
Mulungu pamene machenjezowo atandifika. Ndithudi
Satana ndi wachinyengo nthawi zonse kwa munthu."
30. Mtumwi adati, "Ambuye wanga! Ndithudi anthu anga
alikana Buku la Korani." 31. Motero Ife tapanga kwa
Mtumwi aliyense mdani kuchokera kwa anthu ochimwa,
anthu otsutsana naye, ndipo Ambuye wako ali wokwana
kukhala wokutsogolera mu zabwino ndiponso ngati
wokuthandiza wako.

32. Anthu osakhulupirira anati, "Kodi ndi chifukwa
chiyani Korani yonse siidavumbulutsidwe kwa iye
nthawi imodzi?" Ife talivumbulutsa kotero kuti tikhoza
kulimbikitsa mtima wako ndipo takupatsa ilo kwa iwe
mu chivumbulutso chapang'onopang'ono. 33. Iwo sadzatha
kubwera ndi mtsutso umene Ife sitidakonze yankho loona
ndi kafotokozedwe kake. 34. Iwo adzaduduluzidwa cha
mphumi kupita ku Gahena ndipo iwo adzakhala ndi malo
oipa okhalamo ndipo njira yawo ndi yosochera.

35. Ndithudi Ife tidavumbulutsa mawu a Mulungu kwa
Mose ndipo tidamupatsa m'bale wake Aroni kuti akhale

nduna yomuthandiza. 36. Tidawauza iwo kuti, "Pitani
nonse kwa anthu amene adakana zizindikiro zathu" ndipo
pambuyo pake tidawaononga kotheratu. 37. Akakhala
anthu a Nowa, tidawamiza pamene iwo adakana Atumwi
awo ndipo tidawapanga iwo kukhala phunziro kwa anthu
a mitundu yonse. Ndipo anthu ochimwa tawakonzera
chilango chowawa. 38. Mitundu ya anthu a ku Thamoud
ndi Aad nawonso tidawaononga ndiponso iwo amene anali
kukhala ku Raas ndi mibadwo yochuluka imene idadza
pakati pawo. 39. Ndipo onsewa, tidawapatsa zitsanzo
ndipo onse tidawaononga kotheratu. 40. Ndithudi anthu
osakhulupirira adadutsa pa mzinda umene udaonongeka
ndi madzi a mvula. Kodi iwo sadauone mzindawu? Komabe
iwo adalibe chikhulupiriro mu kuukanso kwa akufa.

41. Nthawi zonse akakuona iwe amakunyoza ndipo
amati, "Kodi uyu ndiye munthu amene akuti Mulungu
wamutumiza ngati Mtumwi wake?" 42. Ngati ife
tikadapanda kulimba popembedza milungu yathu ndithudi
iye akadatitembenuza ife kuti tisiye milungu yathu. Koma
posakhalitsa iwo adzaona chilango ndipo adzadziwa kuti
ndani amene adasochera kwambiri.

43. Kodi wamuona iye amene amayesa zilakolako zake
ngati milungu? Kodi iwe ungakhale munthu wosamalira
munthu wotere? 44. Kodi iwe umaganiza kuti ambiri a iwo
angathe kumva kapena kuzindikira? Iwo si chinthu china
chilichonse koma ali ngati nyama yosochera kwambiri.

45. Kodi iwe siuona mmene Ambuye wako amatambasulira
mthunzi? Mulungu akadafuna, akadaupanga kuti
ukhale wokhazikika. Ndipo Ife tapanga dzuwa kukhala
chizindikiro chake. 46. Ndipo timaubweretsa kwa Ife

mwapang'onopang'ono mosavuta. 47. Ndiye amene wapanga
usiku kukhala chofunda ndi tulo kuti tikhale mpumulo,
ndipo wapanga usana kuti uzikhala nthawi yodzuka
ndi kumagwira ntchito. 48. Ndiye amene amatumiza
mphepo ngati mthenga wobweretsa chisomo chake ndipo
timatumiza madzi abwino kuchokera kumwamba. 49. Ndi
cholinga choti tipereke moyo ku nthaka imene inali yakufa
ndi kuti timwetse zinthu zimene talenga, nyama ndi anthu
ambiri.

50. Ndithudi tawatumizira pakati pawo, kuti akhoza
kukumbukira, chisomo cha Mulungu koma anthu ambiri
amakana. Ndipo iwo amasankha kusakhulupirira.
51. Chikadakhala chifuniro chathu, tikadautsa
wowachenjeza ku mzinda uliwonse. 52. Iwe usawamvere
anthu osakhulupirira koma limbana nawo kwambiri
pogwiritsa ntchito Korani ino.

53. Ndiye amene adatumiza nyanja ziwiri, ina yamadzi
ozuna ndi abwino pamene ina ndi yamadzi a mchere ndi
owawa ndipo adakhazikitsa malire olimba kwambiri
pakati pa nyanjazi. 54. Ndiye amene adamulenga munthu
kuchokera ku madzi ndipo adamupatsa abale chifukwa
cha magazi amodzi ndiponso chifukwa cha ukwati.
Ndipo Ambuye wako ndiye mwini mphamvu zonse ndipo
amachita zimene afuna.

55. Komabe anthu osakhulupirira amapembedza mafano
moonjezera pa Mulungu Mafanowo sangathe kuwathandiza
kapena kuwaononga. Munthu wosakhulupirira
amathandiza Satana kuchita zoipa zosakomera Ambuye
wake. 56. Ndipo takutumiza iwe ngati wobweretsa nkhani
yabwino ndiponso munthu wopereka chenjezo. 57. Nena,

“Ine sindili kukupemphani malipiro pa ntchito iyi ayi
kupatula kuti iye amene afuna atsatire njira yoyenera
yopita kwa Ambuye wake.”
58. Ndipo ika chikhulupiriro chako mwa Iye wa moyo
amene sakufa ayi. Ndipo mulemekeze nthawi zonse. Iye ndi
okwana chifukwa Iye amadziwa bwinobwino za machimo
a akapolo ake. 59. Iye adalenga kumwamba ndi dziko
lapansi ndi zonse zimene zili m’menemo masiku asanu ndi
limodzi. Ndipo atatero adabuka pa chimpando chaufumu,
Mwini Chisononi chosatha. Motero mufunse Iye chifukwa
amadziwa china chili chonse. 60. Pamene zimanenedwa kwa
iwo kuti, “Lambirani Mwini chisoni chosatha,” Iwo amati;
“Kodi Mwini chisoni chosatha ndani? Kodi iwe ufuna kuti
ife tizipembedza chilichonse chimene iwe utilamula?”
Mawu amenewa amaonjezera kukana kwawo.
61. Alemekezeke Iye amene adalenga gulu la nyenyezi
kumtambo ndipo adalenga dzuwa ndi mwezi wowala.
62. Ndipo ndiye amene amasinthanitsa usiku ndi usana
chifukwa cha iye amene afuna kukumbukira kapena afuna
kuonetsa kuyamika kwake.
63. Ndipo akapolo a Mwini Chisoni Chosatha ndi
iwo amene amayenda modzichepetsa padziko lapansi
ndipo ngati mbuli zikawayankhula mwachipongwe iwo
amayankha mwaulemu. 64. Ndipo iwo amene amachezera
pamaso pa Ambuye wawo, amagwada ndi kuima.
65. Amene amanena kuti, “Ambuye wathu! Tichotsereni
chilango cha ku Gahena.” Ndithudi chilango chake ndi
chosatha. 66. Ndithudi kumeneko ndi malo wonyansa
kupumirako ndiponso malo wonyansa kukhalako. 67. Iwo
akamapereka saononga chuma chawo moposa muyeso

ndipo saumira koma amakhala pakatikati. 68. Ndipo anthu
amene sapembedza mulungu wina kuonjezera pa Mulungu
weniweni ndipo sakupha mzimu umene Mulungu waletsa
kupatula mu njira yachilungamo ndipo sachita chigololo.
Ndipo aliyense amene achita izi adzalandira chilango.
69. Chilango chake chidzaonjezedwa kawiri patsiku la
kuuka kwa akufa ndipo adzakhala ndi manyazi nthawi
zonse. 70. Kupatula okhawo amene alapa ndi kukhulupirira
ndi kuchita ntchito zabwino, chifukwa potero Mulungu
adzasintha zoipa zawo kukhala ntchito zabwino. Ndipo
Mulungu amakhululukira ndi wachisoni chosatha. 71. Iye
amene alapa ndi kuchita ntchito zabwino, ndithudi, ndiye
kuti wabwerera kwa Mulungu.

72. Iwo amene sapereka umboni ku zinthu zabodza
ndipo akamadutsa pamalo pamene pakuchitika zinthu
zoipa kapena zoletsedwa, iwo amadutsa modzilemekeza.
73. Amene sanyozera chivumbulutso cha Ambuye wawo
ndipo pamene akumbutsidwa za icho sachita ngati kuti
iwo ndi a gonthi kapena a khungu. 74. Ndipo anthu amene
amanena kuti, "Ambuye wathu! Tipatseni chisangalalo mu
akazi ndi ana athu ndipo tipangeni ife kukhala atsogoleri a
iwo amene amakuopani Inu!"

75. Amenewa adzalipidwa Paradiso wa pamwamba
chifukwa cha kupirira kwawo. Kumeneko adzalandiridwa
ndi malonje abwino mawu amtendere ndi aulemu.
76. Adzakhala kumeneko nthawi zonse ndipo ndi malo
abwino kukhalako ndiponso ndi malo abwino opumirako.
77. Nena "Ambuye wanga amakusamalani inu chifukwa cha
mapemphero anu a kwa Iye yekha. Koma tsopano, ndithudi,

inu mwamukana Iye. Motero chilango chidzakhala chanu
mpaka kalekale.”

Sura 26 • Ash-Shu‘arâ

## Al Shuara

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo, Mwini
Chisoni Chosatha.

1. *Ta Sin Mim.*

2. Awa ndi mawu omveka a Buku la Korani. 3. Iwe mwina
ukhoza kudziononga ndi madandaulo chifukwa cha
kusakhulupirira kwawo. 4. Ngati Ife tifuna, tikhoza
kuwavumbulutsira chizindikiro chochokera kumwamba
chimene makosi awo adzakhota modzichepetsa. 5. Palibe
chenjezo latsopano limene limadza kuchokera kwa Mwini
chisoni chosatha koma iwo amalikana. 6. Ndithudi iwo
amakana mawu a Mulungu koma nkhani zidzadza kwa iwo
zokhudza zinthu zimene iwo amazichita chipongwe.
7. Kodi iwo saona nthaka, mmene ife tameretsamo
mbewu zabwino zosiyanasiyana? 8. Ndithudi m’menemu
muli chizindikiro komabe ambiri a iwo sakhulupirira ayi.
9. Ndithudi Ambuye wako ndiye Mwini mphamvu zonse
ndiponso Mwini chisoni chosatha.
10. Ndipo pamene Ambuye wako adamuitana Mose
adanena kuti, “Pita kwa anthu opanda chilungamo.”
11. Kodi anthu a Farawo sangaope? 12. Iye adati, “Ambuye
wanga! Ndithudi ine ndili kuopa kuti adzandikana.”
13. “Ndipo ndikhoza kupsa mtima ndi kulephera kuyankhula.

Tumizani Aroni.” 14. “Ndipo iwo ali ndi mangawa ndi ine
ndipo ndichita mantha kuti akhoza kukandipha.”
15. Mulungu adati, “Nkosatheka kutero! Kotero pitani
nonse awiri ndi zizindikiro zathu. Ife tidzakhala ndi
inu ndipo tidzamva.” 16. Ndipo mukakafika kwa Farawo
mukamuuze kuti, “Ife ndife Atumwi ochokera kwa
Ambuye wa zolengedwa zonse.” 17. “Motero alekeni ana
a Israyeli kuti apite ndi ife.” 18. (Farawo) adati, “Kodi ife
sitidakurere iwe pamene udali wamng’ono? Ndipo iwe
unakhala pakati pathu zaka zambiri.” 19. “Ndipo iwe
udachita chimene udachita. Ndithudi iwe ndiwe mmodzi
wa anthu osathokoza.”
20. (Mose) adati, “Ine ndidachita chimenecho popeza
nthawi imeneyo ndidali wosadziwa china chilichonse.”
21. “Motero ine ndidathawa inu nonse pa nthawi imene
ndidakuopani koma tsopano Ambuye wanga wandipatsa
luntha ndiponso wandipanga ine kukhala mmodzi mwa
Atumwi ake.” 22. “Ndipo uwu ndi mwayi umene ubwino
wake iwe uli kundinyogodola. Iwe wasandutsa ana a Israyeli
kukhala akapolo ako.” 23. Farawo adati, “Kodi Ambuye
wa zolengedwa zonse ndani?” 24. (Mose) adati, “Ambuye
wa kumwamba ndi dziko lapansi ndi zonse zimene zili
pakati pawo ngati inu mufuna kukhulupirira.” 25. (Farawo)
adawafunsa anthu amene adamuzungulira! “Kodi muli
kumva zimene ali kunenazi.” 26. (Mose) adapitiriza kuti,
“Ambuye wanu ndiponso Ambuye wa makolo anu akale.”
27. (Farawo) adati, “Ndithudi Mtumwi amene watumizidwa
kwa inu ndi wopenga.” 28. (Mose) adati, “Iye ndi Ambuye
wa kum’mawa ndi kumadzulo ndi zonse zimene zikhala
kumeneko ngati muli ozindikira.” 29. (Farawo) adayankha

kuti, “Ngati iwe utumikira mulungu wina kupatula
ine, ndithudi ndikupanga kukhala mmodzi wa anthu
okhala ku ndende.” 30. (Mose) adafunsa kuti, “Kodi
zingakhale choncho ngakhale nditakulangiza chizindikiro
choonekeratu? “ 31. (Farawo) adati, “Tilangize chizindikiro
chako ngati zonse zimene unena ndi zoona.” 32. Motero
Mose adaponya ndodo yake pansi ndipo nthawi yomweyo
idasanduka njoka yeniyeni. 33. Ndipo Iye adatulutsa dzanja
lake ndipo nthawi yomweyo lidasanduka loyera kwa
iwo amene adaliona. 34. Farawo adauza nduna zake kuti,
“Ndithudi munthu uyu ndi wodziwa matsenga.” 35. “Iyeyu
afuna kukuchotsani m’dziko lanu ndi matsenga ake. Kodi
ulangizi wanu ndi wotani ndipo ukupereka langizo lanji?”

36. Iwo adati, “Muyambe mwawasunga iye pamodzi ndi
m’bale wake kwa kanthawi kochepa. Tumizani mithenga
ku mizinda yanu. 37. Abweretse kwa inu munthu aliyense
yemwe ndi wodziwa matsenga kwambiri.” 38. Motero
anthu amatsengawa adasonkhanitsidwa patsiku lodziwika
lomwe adagwirizana 39. Ndipo anthu adafunsidwa kuti,
“Kodi nonse mudzasonkhana?” 40. “Kuti mwina ife tikhoza
kudzatsatira a matsenga ngati iwo atapambana.” 41. Ndipo
pamene anthu onse amatsenga adadza kwa Farawo, iwo
adati kwa Farawo, “Kodi mudzatilipira ngati titapambana?”
42. Iye adati, “Inde. Ndipo ndithudi inu mudzakhala kufupi
ndi Ine.”

43. Mose adawauza kuti, “Ponyani pansi chilichonse
chimene mufuna kuponya.” 44. Ndipo iwo adaponya zingwe
ndi ndodo zawo ndipo adati: “Mwa mphamvu ya Farawo,
ndithudi, ife tipambana.” 45. Ndipo Mose adaponya ndodo
yake ndipo nthawi yomweyo idameza zonse zabodza

zimene iwo adapanga. 46. Ndipo anthu amatsenga onse aja
adagwa pansi mogwada. 47. Iwo adati, “Ife takhulupirira
mwa Ambuye wa zolengedwa zonse.” 48. “Ambuye wa Mose
ndi Aroni”
49. Farawo adati, “Kodi inu mwakhulupirira mwa iye
pamene ine sindinakupatseni chilolezo? Ndithudi iye
ndi mtsogoleri wanu amene adakuphunzitsani matsenga.
Ndithudi posachedwapa mudzazindikira. Ndithudi ine
ndidzadula manja anu ndi miyendo yanu moisiyanitsa.
Ndidzakudulani dzanja lamanja ndi mwendo wamanzere
ndiponso ndidzakupachikani pa mtanda.” 50. Iwo adati,
“Zilibe kanthu chifukwa ndithudi ife tidzabwerera kwa
Ambuye wathu.” 51. “Ndithudi Ife tili ndi chiyembekezo
kuti Ambuye wathu adzatikhululukira machimo athu
popeza ndife oyamba kukhulupirira.”
52. Ndipo tidamulamula Mose kuti, “Nyamuka nthawi
ya usiku ndi akapolo anga chifukwa, ndithudi, inu
mulondoledwa ndi gulu la adani anu.” 53. Ndipo Farawo
adatumiza mithenga ku mizinda yonse. 54. “Ndithudi
anthu amenewa ndi kagulu ka anthu ochepa.” 55. “Ndithudi
anthu amenewa atipsetsa mtima.” 56. “Ife tonse tili
tcheru.” 57. Ndipo tidawachotsa m’minda ndi mu a kasupe.
58. Ndiponso m’chuma ndi m’malo alionse olemekezeka.
59. Kotero tidawapanga ana a Israyeli kukhala alowa m’malo
a zinthu za anthu a Farawo.
60. Pamene dzuwa linali kutuluka, iwo adalondoledwa
ndi adani awo. 61. Ndipo pamene magulu awiriwa adaonana
wina ndi mnzake, anthu a Mose adati, “Ndithudi atipeza.”
62. Mose adati, “Iyayi. Ndithudi Ambuye wanga ali ndi ine
ndipo adzanditsogolera.” 63. Ndipo tidalamulira Mose kuti,

“Menya madzi a m’nyanja ndi ndodo yako.” Ndipo nyanja
idagawanika pakati, mbali iliyonse idali ngati phiri lalikulu.
64. Ndipo anthu a Farawo tidawayandikitsa ndi nyanja
ija. 65. Ndipo Ife tidapulumutsa Mose ndi onse amene
adali ndi iye. 66. Ndipo tidamiza ena. 67. Ndithudi mu ichi
muli phunziro komabe anthu ambiri sakhulupirira ayi.
68. Ndithudi Ambuye wako! Iye ndiye Mwini mphamvu
zonse ndi Mwini chisoni chosatha.

69. Ndipo afotokozere nkhani za Abrahamu. 70. Pamenepo
iye adanena kwa abambo ake ndiponso kwa anthu ake
kuti, “Kodi ndi chiyani chimene inu muli kupembedza?”
71. Iwo adati, “Timatumikira mafano ndipo timapempha
kwa iwo modzipereka kwambiri.” 72. Ndipo adati, “Kodi
iwo amakumvani pamene mumawapempha?” 73. “Kodi
amakuthandizani kapena kukuonongani?” 74. Iwo adati,
“Iyayi. Koma ife tidawapeza makolo athu akupembedza
mafano.”

75. Iye adati, “Kodi inu muli kuzidziwa zimene muli
kuzipembedza?” 76. “Inu ndiponso makolo anu akale?”
77. “Ndithudi onse ndi adani anga kupatula Ambuye
wachilengedwe.” 78. “Amene adandipanga ine ndipo
ndiye amene amandipatsa chilangizo.” 79. “Ndipo ndiye
amene amandipatsa chakudya ndi chakumwa.” 80. “Ndipo
ndikadwala, ndi Iye amene amandichiza.” 81. “Ndipo ndiye
amene adzandipangitsa kuti ndife ndi kudzandibwezeranso
moyo.” 82. “Ndi amene ine ndimayembekezera kuti
adzandikhululukira machimo anga pa tsiku lachiweruzo”

83. Ambuye ndipatseni luntha ndipo mundilole kuti
ndikhale pakati pa anthu ochita zabwino. 84. Ndipatseni
ulemerero umene udzatchulidwe ndi mibadwo yomwe

ikubwera mtsogolo. 85. Ndipo ndiikeni m'gulu la anthu
amene adzakhala kumalo a mtendere a ku Paradiso.
86. Akhululukireni abambo anga ndithudi iwo ali mmodzi
mwa anthu osochera. 87. Musadzandichititse manyazi
patsiku limene anthu adzaukitsidwa kwa akufa. 88. Tsiku
limene chuma ndi ana sizidzathandiza wina aliyense
89. Kupatula yekhayo amene adzadza kwa Mulungu ndi
mtima woyera 90. Pamenepo Paradiso idzayandikiritsidwa
kwa anthu angwiro. 91. Ndipo Gahena idzaonetsedwa
poyera kwa anthu ochimwa. 92. Mawu adzanenedwa kwa
iwo kuti, "Kodi mafano anu aja amene mumatumikira
ali kuti?" 93. Kuwonjezera pa Mulungu weniweni? Kodi
iwo akhoza kukuthandizani inu kapena kudzithandiza
okha?" 94. Ndipo iwo ndi onse ochimwa adzaponyedwa
ku Gahena,, 95. Ndiponso pamodzi ndi magulu onse a
Satana. 96. Iwo adzati pamene adzakhala ali kukangana
kumeneko, 97. "Pali Mulungu, ndithudi, ife tidali ochimwa
moonekeratu." 98. Pamene tidakusandutsani inu kukhala
ofanana ndi Ambuye wa zolengedwa zonse.

99. Palibe ena koma anthu ochita zoipa amene
adatisocheretsa ife. 100. Palibe wina woti angatipepesere
ife. 101. Ndiponso palibe bwenzi lenileni. 102. Koma
tikadakhalanso ndi moyo, tikadakhala anthu okhulupirira.
103. Ndithudi mu zimenezi muli chizindikiro koma anthu
ambiri sakhulupirira ayi. 104. Ndithudi Ambuye wanu!
Ndiye Mwini mphamvu zonse ndi Mwini chisoni chosatha.

105. Anthu a m'badwo wa Nowa adakana Atumwi awo.
106. Pamene Nowa adati, "Kodi inu simungaope Mulungu
ndi kumumvera Iye?" 107. "Ndithudi ine ndine Mtumwi
wanu wokhulupirika." 108. "Motero opani Mulungu ndipo

mundimvere ine.” 109. “Ine sindikupemphani malipiro ena
alionse chifukwa palibe wina aliyense amene angandilipire
ine kupatula Ambuye wa zolengedwa zonse.” 110. “Kotero
opani Mulungu ndipo mundimvere ine.” 111. Iwo adati,
“Kodi ife tikukhulupirire iwe pamene anthu onyozeka
ndiwo amene amakutsatira iwe?” 112. Nowa adati, “Kodi
ine ndikudziwa chiyani za chimene iwo amachita?”
113. “Ambuye wanga ndiye amene akhoza kuweruza ngati
mumazindikira.” 114. “Ndipo ine sindidzathamangitsa
anthu okhulupirira moona.” 115. “Ine ndine wopereka
chenjezo poyera.”

116. Iwo adati, “Iwe Nowa; ngati siusiya zimene uchita
udzaponyedwa miyala.” 117. Iye adati, “Ambuye wanga!
Ndithudi anthu anga akundikana.” 118. Motero weruzani
mwachilungamo pakati pa ine ndi iwo. Ndipulumutseni
ine pamodzi ndi anthu okhulupirira amene ali ndi ine.
119. Ife tidamupulumutsa iye pamodzi ndi iwo amene adali
naye m’chombo. 120. Ndipo pambuyo pake tidamiza ena
onse ndi chigumula. 121. Ndithudi mu chimenechi muli
phunziro komabe ambiri sakhulupirira. 122. Ndithudi
Ambuye wako ndi Mwini mphamvu ndi Mwini chisoni
chosatha.

123. Anthu a ku Aad sanakhulupirire Atumwi awo.
124. Pamene m’bale wawo Houd adati, “Kodi inu
simungakhale ndi mantha ndi Mulungu?” 125. “Ndithudi
ine ndine Mtumwi wanu wokhulupirika.” 126. “Opani
Mulungu ndipo munditsate ine.” 127. “Pa ntchito iyi, ine
sindipempha malipiro kuchokera kwa inu chifukwa
palibe wina amene angandilipire kupatula Ambuye wa
zolengedwa zonse.” 128. “Kodi inu mukumamanga nyumba

pamalo paliponse pokwera mofuna kudzisangalatsa?”
129. “Kodi muli kumanga nyumba zokongola ndi zolimba
ngati kuti mudzakhalamo mpaka kalekale?” 130. “Ndipo
pamene mumenya anthu mumamenya ngati anthu
ankhanza.” 131. “Motero opani Mulungu, ndipo mundimvere
ine.” 132. “Ndipo muopeni Iye amene wakupatsani inu
zinthu zonse zimene mumazidziwa.” 133. “Iye wakupatsani
nyama ndi ana,” 134. “Ndiponso minda ndi a kasupe;”
135. “Ndithudi ine ndili kuchita mantha ndi chilango
chimene chidzadza pa inu pa tsiku loopsa.”

136. Iwo adati, “Ndi chimodzimodzi kwa ife kaya
utilalikira kapena ayi.” 137. “Zonse zimene uli kutiopseza
nazo ndi chikhalidwe cha anthu amakedzana.” 138. “Ife
sitidzalangidwa ayi.” 139. Iwo adamukana iye ndipo Ife
tidawaononga onse. Ndithudi mu chimenechi muli
phunziro koma ambiri sakhulupirira ayi. 140. Ndithudi
Ambuye wako ndiye Mwini mphamvu zonse ndi Mwini
chisoni chosatha.

141. Anthu a Thamoud adakana Atumwi awo. 142. Pamene
m’bale wawo Saleh adati, “Kodi inu simungakhale ndi
mantha ndi Mulungu?” 143. “Ndithudi ine ndine Mtumwi
wanu okhulupirika.” 144. “Motero opani Mulungu
ndipo mundimvere ine.” 145. “Pa ntchito iyi ine sindili
kukupemphani malipiro. Palibe wina amene angandilipire
kupatula Ambuye wa zolengedwa zonse.” 146. “Kodi inu
muganiza kuti mudzasiyidwa mu mtendere wa m’dziko
lino?” 147. “M’kati mwa minda ndi a kasupe.” 148. “Minda
ya chimanga ndi mitengo ya tende imene yapatsa zipatso
zambiri.” 149. “Ndipo muboola mapiri ndi kumangamo
nyumba zanu mwaukatswiri;” 150. “Khalani ndi mantha

ndi Mulungu ndipo mundimvere ine.” 151. “Musamvere
malamulo a anthu oononga.” 152. “Amene amachita zoipa
padziko lapansi ndipo sakonza makhalidwe awo.”
153. Iwo adati, “Iwe uli mmodzi mwa olodzedwa.” 154. “Iwe
ndiwe munthu wonga ife tomwe. Tilangize chizindikiro
ngati zimene ukunenazi ndi zoona” 155. Iye adati, “Iyi ndi
ngamira yaikazi. Iyo idzamwa madzi patsiku lake ndipo inu
mudzamwa patsiku lanu lokhazikitsidwa.” 156. “Musaizunze
ayi chifukwa mukatero chilango cha tsiku loopsa
chidzadza kwa inu.” 157. Komabe iwo adaipha iyo ndipo
adanong’oneza bombono. 158. Chilango chidawapeza iwo.
Ndithudi mu chimenechi muli chizindikiro koma ambiri
a iwo sakhulupirira. 159. Ndithudi Ambuye wako! Indedi
ndiye Mwini mphamvu zonse ndi Mwini chisoni chosatha.
160. Anthu a Loti adakana Atumwi awo. 161. Pamene
m’bale wawo Loti adati, “Kodi inu simungaope Mulungu?”
162. “Ndithudi ine ndine Mtumwi wanu wokhulupirika.”
163. “Opani Mulungu ndipo mundimvere ine.” 164. “Ine
sindili kupempha kuti mundilipire chifukwa cha ichi
ayi chifukwa palibe wina amene angandilipire kupatula
Ambuye wa zolengedwa zonse.” 165. “Kodi inu mwasankha
kuti muzigonana ndi amuna anzanu mwa zolengedwa
zonse? 166. “Kusiya akazi amene Mulungu adakulengerani?
Koma inu ndinu anthu olakwa kwambiri.”
167. Iwo adati, “Iwe Loti! Ngati siusiya zimenezi ndithudi
udzakhala mmodzi mwa othamangitsidwa.” 168. Iye adati,
“Ine ndili kudana ndi makhalidwe anu.” 169. “Ambuye wanga!
Ndipulumutseni ine pamodzi ndi a pabanja langa ku ntchito
zawo zoipa.” 170. Ndipo Ife tidamupulumutsa iye pamodzi
ndi anthu ake onse. 171. Kupatula mayi wokalamba, pakati

pa amene adatsalira m'mbuyo. 172. Ndipo Ife tidawaononga
kwambiri ena onse. 173. Ndipo choipa chidali chilango cha
mvula imene idagwa pa iwo amene adachenjezedwa koma
sadamvere. 174. Ndithudi mu ichi muli phunziro koma
ambiri a iwo sakhulupirira. 175. Ndithudi Ambuye wako
ndiye mwini mphamvu zonse ndi mwini chisoni chosatha.

176. Nawonso anthu okhala m'nkhalango adakana Atumwi.
177. Pamene Shaibu adawauza kuti, "Kodi inu simungaope
Mulungu?" 178. "Ndithudi ine ndine Mtumwi wanu
wokhulupirira." 179. "Opani Mulungu ndipo mundimvere
ine." 180. "Ine sindikupemphani malipiro chifukwa palibe
wina aliyense amene angandilipire kupatula Ambuye
wa zolengedwa zonse." 181. "Perekani muyeso oyenera
ndipo musachepetse." 182. "Yesani ndi miyeso yabwino."
183. "Ndipo musawachepetsere anthu zinthu zawo kapena
kulowetsa chisokonezo m'dziko." 184. "Muopeni Iye amene
adakulengani inu ndi mibadwo yakale."

185. Iwo adati, "Ndithudi iwe walodzedwa." 186. "Iwe
ndiwe munthu wolingana ndi ife. Ndithudi ife tili kuganiza
kuti iwe uli kunama." 187. "Tigwetsere mtambo kuchokera
kumwamba ngati zimene uli kunena ndi zoonadi."
188. Iye adati, "Ambuye wanga amadziwa kwambiri chimene
inu mumachita." 189. Iwo adamukana iye kotero chilango
cha thambo ndi moto chidawaononga. Ichi chidali
chilango cha tsiku loopsa. 190. Ndithudi mu chimenechi
muli chiphunzitso koma ambiri a iwo sakhulupirira.
191. Ndithudi Ambuye wako ndiye Mwini mphamvu zonse
ndi Mwini chisoni chosatha.

192. Buku lolemekezekali lavumbulutsidwa ndi Ambuye
wa zolengedwa zonse. 193. Mzimu wokhulupirika

udabweretsa Bukuli. 194. Ku mtima wako kuti ukhoza kuchenjeza mitundu ya anthu. 195. Mu chinenero chomveka cha Chiarabu. 196. Ndithudi lili kupezeka mu mawu a Mulungu akale. 197. Kodi si chizindikiro kwa iwo kuti anthu ophunzira a ana a Israyeli amalidziwa?

198. Ngati Ife tikadaivumbulutsa kwa munthu wa mtundu wina uliwonse yemwesi wa Chiarabu. 199. Kuti iye ailakatule kwa iwo ndipo sakadakhulupirira iwo mwa Bukulo. 200. Kotero Ife tidaipanga iyo kuti ilowe m’mitima ya anthu ochita zoipa. 201. Iwo sadzakhulupirira mu ilo mpaka pamene adzaona chilango chowawa. 202. Ndipo icho chidzadza kwa iwo mwadzidzidzi pamene iwo sakudziwa 203. Ndipo iwo adzati, “Kodi ife sitidzapatsidwanso nthawi?”

204. Kodi iwo angafune kuti chilango chathu chidze msanga? 205. Tandiuza. Ngati Ife titawalola kukhala mu mtendere wa zaka zambiri. 206. Ndipo pambuyo pake chilango chimene chidalonjezedwa chidza pa iwo. 207. Chisangalalo chawo chimene adapatsidwa chidzakhala chopanda phindu 208. Palibe mtundu wa anthu umene tidaonongapo kale umene sitidautumizire owachenjeza. 209. Monga chenjezo ndipo Ife si ndife opondereza ayi. 210. Si a Satana amene adabweretsa Korani ino ayi. 211. Si koyenera kwa iwo ndiponso sangathe kutero. 212. Ndithudi iwo amanidwa kumva za Bukuli.

213. Musapembedze milungu ina kuonjezera pa Mulungu weniweni chifukwa mukatero mudzakhala m’gulu limene lidzalangidwa. 214. Achenjeze abale ako amene ali pafupi ndi iwe. 215. Ndipo onetsa chifundo kwa anthu okhulupirira amene amakutsatira iwe. 216. Ngati iwo sakumvera iwe, unene kuti, “Ine sindidzaimbidwa mlandu chifukwa cha

zimene mumachita.” 217. Ika chikhulupiriro chako mwa
Mwini mphamvu zonse ndi Mwini chisoni chosatha.
218. Amene amakuona pamene umaimirira popemphera.
219. Ndi machitidwe ako pakati pa anthu opemphera.
220. Mulungu amamva chilichonse ndipo amadziwa china
chilichonse

221. Kodi ndi kuuzeni za munthu amene Satana
amamutsikira? 222. Iwo amadza pa munthu wabodza ndi
wochimwa. 223. Iwo amamvera mabodza okhaokha ndipo
koma ambiri a iwo ndi a bodza. 224. Alakatuli amatsatidwa ndi
anthu ochita zoipa. 225. Kodi simuona kuti iwo amangonena
nkhani iliyonse mu zolakatula zawo? 226. Ndipo iwo
amakamba zinthu zimene iwo sachita 227. Kupatula okhawo
amene akhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino
ndi kumakumbukira Mulungu kwambiri ndi kudziteteza
pambuyo pa kuponderezedwa. Ndipo iwo amene amachita
zoipa adzadziwa chimene chidzawagadabuza.

Sura 27 • An-Naml

# Al Naml

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ichi ndi chivumbulutso cha Korani, Buku lofotokoza
bwino. 2. Malangizo ndi nkhani yosangalatsa kwa anthu
okhulupirira. 3. Amene amapitiriza kupemphera ndipo
amapereka msonkho wothandiza anthu osauka ndiponso
amakhulupirira kwambiri m’moyo umene uli nkudza.

4. Ndithudi iwo ndi amene amakana za moyo umene uli
nkudza. Ife tazipanga ntchito zawo kuti zioneke ngati
zabwino motero iwo amayenda mwakhungu. 5. Iwo
adzalangidwa koposa. Ndipo m'moyo umene uli nkudza,
iwo sadzapindula china chilichonse. 6. Ndithudi iwe
walandira Korani kuchokera kwa Iye amene ali ndi nzeru
ndipo amadziwa chilichonse.
7. Pamenepo Mose adauza banja lake kuti, "Ine ndili
kuona moto. Ine posachedwapa ndikubweretserani nkhani
kapena khala la moto kuti mukhoza kuotha." 8. Ndipo
pamene iye adafika pamoto paja, mawu adamveka akunena
naye kuti, "Odalitsidwa ndiye amene ali mu moto uwu
ndiponso alionse a pamalo pozungulira. Ulemerero ukhale
kwa Mulungu, Ambuye wa zolengedwe zonse."
9. "Mose! Ine ndine Mulungu, Mwini mphamvu zonse
ndi Mwini nzeru zonse." 10. "Ponya ndodo yako pansi."
Ndipo pamene iye adaona kuti ilikuyenda ngati njoka,
adatembenuka ndi kuthawa ndipo sadayang'ane m'mbuyo.
"Iwe Mose!" Atumwi anga sachita mantha pamene ali ndi
Ine. 11. Akakhala iwo amene amalakwa ndipo amachita
zabwino pambuyo pochita zoipa Ine ndine wokhululukira
ndiponso wachisoni chosatha. 12. "Pisa dzanja m'thumba
mwako. Litulutse lili loyera ngakhale kuti siudapweteke.
Ichi ndi chimodzi cha zizindikiro zisanu ndi zinayi zimene
zidzaonetsedwa kwa Farawo ndi anthu ake. Ndithudi iwo
ndi anthu ochimwa kwambiri." 13. Pamene zizindikiro
zathu zooneka bwino zinaonetsedwa kwa iwo, iwo adati,
"Uwu ndiwo ufiti weniweni." 14. Mitima yawo idadziwa
kuti zizindikiro zidali zoona koma adazikana izo chifukwa

chakulakwa ndiponso kunyada kwawo. Taona zimene
zidawaonekera anthu olakwa.
15. Ndithudi Ife tidapereka nzeru kwa Davide ndi
Solomoni. Iwo adati, "Kuyamikidwa ndi kwa Iye amene
watikweza ife kukhala pamwamba pa akapolo ake ambiri
okhulupirira." 16. Solomoni adalowa m'malo mwa Davide. Iye
adati, "Oh inu anthu anga! Ife taphunzitsidwa chiyankhulo
cha mbalame ndipo tapatsidwa zinthu zabwino zambiri.
Ndithudi ichi ndi chifundo choonekeratu."
17. Asirikali a nkhondo a mtundu wa majini, anthu ena
ndi mbalame anasonkhanitsidwa pamaso pa Solomoni
ndipo adaimitsidwa pa mizere m'magulu osiyanasiyana
mogwirizana ndi maudindo. 18. Mpaka pamene iwo
anafika pa chigwa cha nyerere, nyerere ina idati, "Oh inu
nyerere! Lowani ku maenje anu chifukwa mwina Solomoni
pamodzi ndi Asirikali ake, akhoza kukuonongani
mosadziwa." 19. Solomoni adamwetulira posangalatsidwa
ndi mawu ake ndipo iye adati, "Ndilangizeni Ambuye kuti
ndizikuthokozani pa zabwino zonse zimene mwandipatsa
ine ndi makolo anga ndiponso kuti ndizichita ntchito
zabwino zimene zimakukondweretsani inu. Ndilowetseni
ine ku Paradiso kudzera m'chisomo chanu, kuti ndikhale
pakati pa akapolo anu angwiro."
20. Iye adayendera mbalame nati, "Kodi mbalame
yotchedwa mnthengu ili kuti? Kodi kapena iyo ili pamodzi
ndi amene sadabwere?" 21. "Ndithudi ndidzailanga iyo
ndi chilango chowawa kapena ndidzaipha kupatula
ngati ibweretsa kwa ine chifukwa chomveka."
22. Ndipo mbalame ya mnthengu siidachedwe ndipo idati,
"Ndadziwa zimene iwe siudziwa ndipo ndikubweretsera

nkhani yoona kuchokera ku Saba.” 23. “Ine ndapeza munthu
wamkazi akulamulira iwo ndipo iye wapatsidwa zinthu
zonse zomuyenereza ndipo ali ndi Mpando waukulu
wachifumu. 24. Ndidamupeza iye pamodzi ndi anthu ake
ali kupembedza dzuwa moonjezera pa Mulungu ndipo
Satana wawakongoletsera ntchito zawo zoipa ndipo
wawasocheretsa ku njira yoyenera ndipo iwo si otsogozedwa
bwino.” 25. Ndi kuti sapembedza Mulungu amene amaulula
zobisika za kumwamba ndi pa dziko lapansi ndipo Iye
amadziwa zimene inu mumabisa ndi zimene mumaulula.
26. Mulungu! Kulibe mulungu wina koma Iye yekha.
Ambuye wa mpando wa Chifumu.
27. Solomoni adati, “Tidzaona posachedwapa ngati
zimene ukunena ndi zoona kapena zabodza.” 28. “Pita
ukapereke kalata yangayi kwa iwo ndipo ukachoke
pang’ono poyembekezera yankho lawo.” 29. Mfumukazi ya
ku Saba adati, “Oh inu nduna zanga! Ine ndalandira kalata
yolemekezeka.” 30. Kalatayi ndi yochokera kwa Solomoni
ndipo ikuti, “M’dzina la Mulungu, Mwini chifundo ndi
Mwini chisoni chosatha.” 31. “Usadzikweze kwa ine koma
bwerani nonse kwa ine modzipereka.” 32. Iye adati, “Oh
inu mafumu! Ndipatseni chilangizo chokhudza nkhani
iyi ndipo sindilamula china chilichonse pokhapokha
inu mutakhalapo.” 33. Iwo adati, “Ife ndife olimba mtima
ndiponso odziwa kumenya nkhondo molimba, ndipo
nkhani ili kwa iwe. Ndipo udziwe mmene ungalamulire.”
34. Iye adati, “Ndithudi mafumu akalowa mu mzinda
amaononga mwaupandu ndi kuwasandutsa anthu
olemekezeka kukhala onyozeka. Umo ndi mmene iwo
amachitira.” 35. “Koma ine ndiwatumizira mphatso ndipo

ndidzaona yankho limene a Kazembe anga adzabwere
nalo.”
36. Ndipo pamene akazembe adadza kwa Solomoni,
iye adati, “Kodi muli kundipatsa chuma chambiri? Icho
chimene Mulungu wandipatsa ine ndi chabwino kuposa
chuma chonse chimene wakupatsani inu. Koma inu
mumasangalala ndi mphatso zanu.” 37. “Bwererani kwa iwo.
Ife tidzapita kwa iwo ndi magulu ankhondo amene iwo
sangathe kuwagonjetsa ndipo tidzawathamangitsa m’dziko
lawo mochititsa manyazi ndipo iwo adzanyozeka.”
38. Iye adati, “Oh inu mafumu! Kodi ndani amene
angandibweretsere mpando wake wachifumu iwo
asanabwere kwa ine mogonja?” 39. Wina wamphamvu, amene
adali mmodzi wa majini adati, “Ine ndidzakubweretserani inu
musadanyamuke pa mpando wanu. Ine ndili ndi mphamvu
zonyamulira mpando ndiponso ndine wokhulupirika.”
40. Koma wina amene anali kudziwa Mawu a Mulungu adati
“Ine ndidzakubweretserani msanga musadaphenire maso
anu.” Ndipo pamene iye adaona kuti mpando wabwera
kwa iye adati, “Ichi ndi chisomo cha Ambuye wanga kuti
andiyese ngati ndikuthokoza kapena sindikuthokoza.
Ndipo aliyense amene athokoza atero podzipezera yekha
zabwino. Ndipo amene sathokoza ndithu, Ambuye wanga
ali ndi zonse ndipo ndi Wolemekezeka.”
41. Ndipo iye adati, “Sinthani mpando wake wachifumu
kuti tione ngati iye akhoza kuuzindikira kapena ayi.”
42. Ndipo pamene mfumukazi inadza kwa Solomoni
idafunsidwa kuti, “Kodi mpando wako wachifumu ndi
otere?” Iye adati, “Ukukhala ngati umenewu” ndipo ife
tinadziwa kale ndipo tagonja kwa Mulungu mwamtendere.”

43. Zinthu zimene amapembedza zoonjezera pa Mulungu
ndi zimene zamusokoneza. Iye adali mmodzi wa anthu
osakhulupirira. 44. Iye adauzidwa kuti, "Lowa mnyumba
yachifumu." Ndipo pamene iye anaiona iyo, adaganiza kuti
ndi dziwe la madzi ndipo miyendo yake adaionetsa poyera.
Solomoni adati, "Iyi ndi nyumba yachifumu yomatidwa
ndi magalasi." Iye adati, "Ambuye, ine ndalakwira mzimu
wanga. Tsopano ndili kudzipereka pamodzi ndi Solomoni
kwa Mulungu, Ambuye wazolengedwa zonse."

45. A Thamoud, ndithudi, tidawatumizira m'bale wawo
Saleh, amene adati, "Muzipembedza Mulungu basi." Koma
iwo adagawikana m'magulu awiri okangana. 46. Iye adati,
"Anthu anga! Kodi bwanji mufuna kubweretsa choipa
msanga musanabweretse chabwino? Nanga ndi chifukwa
chiyani simupempha chikhululukiro kwa Mulungu kuti
mukhoza kupeza chisomo chake?" 47. Iwo adati, "Ife tili
kuona choipa chochokera kwa iwe ndiponso kwa anthu
amene amakutsatira iwe." Iye adati, "Choipa chimene muli
kuchiona chili kuchokera kwa Mulungu. Inu ndinu anthu
amene muli kuyesedwa."

48. M'mizinda mwawo mudali anthu asanu ndi anayi
amene anali kuchita zoipa mdziko ndipo samachita
zabwino ayi. 49. Iwo adati, "Tiyeni tonse tilumbire, dzina
la Mulungu, kuti timuphe nthawi ya usiku pamodzi ndi a
pabanja lake lonse. Ndipo tidzawauza abale ake kuti, "Ife
kudalibe pamene iwo anali kuphedwa. Ndipo zimene tili
kunena ndi zoona zokhazokha." 50. Iwo adachita chiwembu
ndipo nafenso tidachita chiwembu iwo osadziwa
chilichonse. 51. Ndipo taona zotsatira zake za chiwembu
chawo. Ife tidawaonongeratu pamodzi ndi anthu awo

onse. 52. Chifukwa chakuti iwo adalakwa, nyumba zawo
zimene anali kukhalamo tsopano ndi mabwinja. Ndithudi
m'zimenezi muli zizindikiro kwa anthu ozindikira.
53. Ndipo Ife tidapulumutsa anthu onse okhulupirira ndipo
anali kuopa Mulungu.

54. Loti kwa anthu ake, "Kodi inu mukuchita zinthu
zochititsa manyazi pamene muli kuona?" 55. "Kodi inu
muli kuchita chiwerewere ndi amuna anzanu pokwaniritsa
zilakolako zanu ndi kusiya akazi? Inu ndinu mbuli basi."
56. "Yankho lawo silidali lina koma kuti, "Chotsani anthu
a Loti mu mzinda wanu. Awa ndi anthu amene afuna
kudziyeretsa." 57. Ife tidamupulumutsa iye pamodzi
ndi anthu ake kupatula mkazi wake amene adatsalira
m'chilango. 58. Ndipo tidawalasa iwo ndi mvula ya miyala
imene idagwa pa iwo. Ndi mvula yoipa imene idagwera iwo
amene adachenjezedwa 59. Nena, "Kuyamikidwa kukhale
kwa Mulungu ndipo mtendere ukhale pa Atumwi ake
amene Iye wawasankha. Kodi wabwino ndani Mulungu
kapena mafano amene amawapembedza yoonjezera pa
Mulungu?"

60. Kapena wabwino ndi Iye amene adalenga kumwamba
ndi dziko lapansi ndi kukutumizirani mvula kuchokera
kumwamba ndi kubweretsa minda ya chisangalalo? Iwo
sangathe kumeretsa mitengo. Kodi pali milungu ina
yoonjezera pa Mulungu weniweni? Koma iwo ndi anthu
amene amafanizira ena ake kukhala ofanana ndi Mulungu.
61. Kapena Iye amene adakhazikitsa dziko ndi kulithirira ilo
ndi mitsinje ya madzi oyenda; ndipo wakhazikitsa mapiri
pa dziko ndipo waika malire pakati pa nyanja ziwiri. Kodi

pali mulungu wina woonjezera pa Mulungu weniweni?
Koma ambiri a iwo ndi osadziwa.
62. Kapena Iye amene amayankha mapemphero a
munthu opanikizika pamene amupempha Iye ndipo
amamuchotsera mavuto. Ndiyetu amene wakupatsani
dziko lapansi kuti muzikhalamo. Kodi pali mulungu
winanso woonjezera pa Mulungu weniweni? Ndi
zazing'ono zimene mumakumbukira 63. Kapena ndi Iye
amene amakutsogolerani mu mdima pa mtunda kapena
pa nyanja ndipo amatumiza mphepo ngati yonyamula
uthenga wabwino wa chisomo chake. Kodi pali mulungu
winanso woonjezera pa Mulungu weniweni? Mulungu
ndi wapamwamba kuposa zimene amamufanizira nazo.
64. Kapena Iye amene poyambirira adapanga zolengedwa
ndiponso amene adzatidzutsanso kukhala ndi moyo
m'moyo umene uli nkudza ndiponso amene amakupatsani
chakudya kuchokera ku nthaka ndi kumwamba? Kodi pali
mulungu winanso woonjezera pa Mulungu weniweni? Nena,
"Tionetseni chizindikiro chanu ngati zimene mukunenazi
ndi zoonadi."
65. Nena, "Palibe amene ali kumwamba kapena pa dziko
lapansi amene amadziwa zobisika kupatula Mulungu.
Ndiponso anthu sadziwa nthawi imene adzaukitsidwa
kukhalanso ndi moyo." 66. Kodi kuzindikira kwawo m'moyo
umene uli nkudza kwakwaniritsidwa? Iwo ndi okaika pa
zamoyo umene uli nkudza ndipo maso awo ndi otsekeka
pa za iwo. 67. Anthu osakhulupirira adati, "Kodi pamene
ife ndi makolo anthu, tisanduka dothi tidzaukitsidwanso?"
68. "Ndithudi ife tidalonjezedwa ndiponso makolo athu.
Ichi si china ayi koma nkhani zopanda pake za anthu akale."

69. Nena, “Pitani pa dziko lonse lapansi ndipo mukaone
zimene zidawaonekera anthu ochimwa.”
70. Usachite chisoni kapena kuvutika mu mtima chifukwa
cha ziwembu zimene apanga. 71. Ndipo iwo amati, “Kodi
lonjezo limeneli lidzakwaniritsidwa liti ngati zimene muli
kunenazi ndi zoona?” 72. Nena, “Mwina gawo lina la zimene
muli kufuna kuti zidze msanga zili pafupi kudza.” 73. Ndipo,
ndithudi, Ambuye wako ndi wokoma mtima kwa anthu,
koma ambiri a iwo sathokoza ayi. 74. Ndipo, ndithudi,
Ambuye wako amadziwa zonse zimene zimabisika
m’mitima mwawo ndiponso zonse zimene amaulula.
75. Kulibe chinsinsi kumwamba kapena padziko lapansi
chimene sichidalembedwe mu Buku lake lolemekezeka.
76. Buku la Korani lili kuwauza ana a Israyeli zambiri
zimene iwo amatsutsana 77. Ndipo limeneli ndi chenjezo
ndiponso madalitso kwa anthu okhulupirira m’choonadi.
78. Ndithudi Ambuye wako adzaweruza pakati pawo ndi
chiweruzo chake. Iye ndiye Mwini mphamvu zonse ndi
Mwini kudziwa za chinthu china chilichonse. 79. Kotero
iwe ika chikhulupiriro chako mwa Mulungu chifukwa iwe
uli pa choonadi chenicheni. 80. Ndithudi iwe siungathe
kumupanga munthu wakufa kuti amve ndiponso siungathe
kumupanga munthu osamva kuti amve kuitana kwako
pamene iye atembenuka. 81. Si udindo wako kutsogolera
anthu a khungu kuti aleke kusochera. Palibe munthu amene
adzakumvera kupatula okhawo amene amakhulupirira mu
chivumbulutso chathu ndipo amadzipereka kwathunthu.
82. Patsiku limene chiweruzo chathu chidzayandikira kwa
osakhulupirira, Ife tidzawabweretsera chinyama chimene
chidzayankhula nawo kuchokera ku dziko lapansi chifukwa

munthu sanakhulupirire chivumbulutso chathu. 83. Patsiku
limeneli, tidzasonkhanitsa kuchokera ku mtundu uliwonse
gulu la anthu amene sadakhulupirire chivumbulutso chathu.
Iwo adzasonkhanitsidwa ndi kuikidwa m'mizere 84. Mpaka
pamene adzafike pamalo a chiweruzo, Mulungu adzati,
"Kodi inu mudakana chivumbulutso changa ngakhale kuti
inu simumadziwa chilichonse cha chivumbulutsocho?
Kodi ndi chiyani mumachita?" 85. Chionongeko chidzadza
pa iwo chifukwa cha zoipa zawo ndipo iwo adzasowa
chowiringula. 86. Kodi iwo saona mmene tidakonzera
usiku kuti ukhale mpumulo ndi masana kuti uziwapatsa
kuwala? Ndithudi mu zimenezi muli zizindikiro kwa anthu
okhulupirira.

87. Patsiku limeneli, lipenga lidzalizidwa ndipo onse amene
amakhala kumwamba ndi padziko lapansi adzagwidwa
ndi mantha kupatula okhawo amene Mulungu adzafuna
kuwapatula mu zimene zi. Onse adzabwera kwa Iye
modzichepetsa. 88. Iwe udzaona mapiri ndi kuwaganizira
kuti ndi okhazikika koma iwo adzayenda ngati mmene
mitambo imachitira. Uwu ndi mchitidwe wa Mulungu
amene wakonza bwino lomwe chinthu chilichonse.
Ndithudi Iye amadziwa bwino zonse zomwe mumachita.
89. Iwo amene achita zabwino adzalandira mphotho imene
ili yabwino ndipo adzakhala osakhudzidwa ndi zochititsa
mantha za tsiku limeneli. 90. Koma iwo amene achita zoipa
adzaduduluzidwa pa mphumi zawo kunka ku moto. "Kodi
inu simudzalandira malipiro ofanana ndi ntchito zanu?"

91. Nena, "Ine ndalamulidwa kutumikira Ambuye wa
mzinda uno umene waupanga kuti ukhale Woyera. Zinthu
zonse ndi zake. Ndipo ndalamulidwa kukhala mmodzi

mwa odzipereka.” 92. Ndipo ndalamulidwa kuwerenga
Buku la Korani. Aliyense amene atsatira njira yoyenera
atero podzithandiza yekha. Kwa iye amene asochera
nena “Ine si ndine kanthu kena koma mmodzi wa iwo
ochenjeza anthu.” 93. Ndipo nena, “Kuyamikidwa kukhale
kwa Mulungu! Iye adzakulangizani zizindikiro zake ndipo
inu mudzazizindikira. Ambuye wanu saiwala zimene
mumachita.”

Sura 28 • Al-‘Kasas

# Al Qasas

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni chosatha.

1. *Ta Sin Mim.*

2. Awa ndi mawu a m’Buku lofotokoza bwino. 3. Tidzakuuza
zina za mbiri ya Mose ndi Farawo mwachoonadi kuti uuze
anthu okhulupirira. 4. Ndithudi Farawo adadzikweza pa
dziko lapansi ndipo adagawa anthu ake m’magulumagulu
ndipo gulu lina iye anali kulizunza pomapha ana awo
aamuna ndi kusiya ana aakazi. Ndithudi iye adali wochita
zoipa. 5. Koma chidali chifuniro chathu kuti tiwapatse
zabwino anthu amene adali oponderezedwa pa dziko
ndi kuwasandutsa iwo kukhala atsogoleri a anthu ndi
kuwapanga iwo kulowa m’malo mwa ufumu wa Farawo.
6. Ndikuwakhazikitsa m’dziko ndipo tinamupatsa Farawo,
Hamani ndi gulu lawo la nkhondo zimene iwo anali kuopa.
7. Ife tidauza amayi ake a Mose ponena kuti,

"Muyamwitse iye koma ngati ukuda nkhawa za kukhala
kwake mwamtendere, mponye mu mtsinje. Usaope ndipo
usade nkhawa ayi chifukwa Ife tidzamubweretsa iye kwa
iwe ndi kumupanga iye kukhala mmodzi wa Atumwi."
8. Ndipo adamutola iye a banja la Farawo kuti akhoza
kukhala mdani ndiponso madandaulo kwa iwo. Ndithudi
Farawo, Hamani ndi Asirikali awo, onse adali ochimwa.
9. Mkazi wake wa Farawo adati kwa iye, "Mwana uyu akhoza
kubweretsa chisangalalo kwa ine ndi iwe. Musamuphe ayi.
Mwina akhoza kutithandiza kapena tikhoza kumutenga
kuti akhale mwana wathu." Koma iwo sadadziwe chimene
anali kuchita.
10. Mtima wa amayi ake a Mose siumaganiza zina ayi koma
za Mose yekha. Iye akadaulula za iye kukadapanda kuti Ife
tidamupatsa mphamvu kuti apitirize kukhala wokhulupirira
weniweni. 11. Iye adati kwa mlongo wake wa Mose, "Pita
umutsatire." Iye anali kumuona kuchokera patali pamene
iwo sadadziwe ayi. 12. Tsopano Ife tidamupanga kuti azikana
kuyamwa mawere a amayi ena. Mlongo wake adati kwa iwo,
"Kodi ndingakulondorereni banja limene likhoza kumulera
m'malo mwanu ndi kumusamala bwino?" 13. Ndipo
tidamubweretsa iye kwa Amayi ake kuti asangalale, asiye
kudandaula ndiponso kuti adziwe kuti lonjezo la Mulungu
ndi loona. Koma anthu ambiri sachidziwa chimenechi.
14. Ndipo pamene iye adakula msinkhu ndi kukhala munthu
wokwana, tidamupatsa iye luntha ndi nzeru. Mmenemu
ndi mmene timalipirira anthu ochita zabwino.
15. Ndipo Iye adalowa mu mzinda, osaonedwa ndi anthu
ndipo adapeza anthu awiri ali kumenyana, wina adali wa
mtundu wake ndi wina wa mtundu wa adani ake. Munthu

wa mtundu wake adamupempha iye chithandizo kuti
agonjetse mdani wake. Ndipo Mose adamumenya mdani
wake ndi dzanja lake ndipo adamupha. Mose adati, "Iyi
ndi ntchito ya Satana. Ndithudi Iye ndi mdani wa munthu
wosokoneza kwenikweni." 16. Iye adati, "Ambuye! Ine
ndidalakwira mzimu wanga kotero ndikhululukireni."
Ndipo Mulungu anamukhululukira iye chifukwa Iye ndi
Mwini kukhululukira ndi Mwini chisoni chosatha. 17. Iye
adati, "Chifukwa cha chifundo chimene mwandionetsa
Ambuye, ine ndili kulumbira kuti sindidzathandiza wina
aliyense wochita zoipa."
18. M'mawa mwake iye anali kuyenda mu mzinda
ndi mantha poyembekezera mavuto. Munthu uja,
amene amamuthandiza cha dzulo, adamuitananso kuti
amuthandize. Mose adati, "Ndi choonekeratu kuti iwe
ndiwe munthu wosokoneza." 19. Ndipo pamene Mose
ankati azim'menya mdani uja, munthuyo adati, "Iwe Mose!
Kodi ufuna kundipha monga momwe unaphera munthu
uja dzulo? Ndithudi iwe ufuna kukhala munthu wankhanza
m'dziko lino ndiponso iwe siufuna kukhala mmodzi mwa
anthu angwiro." 20. Ndipo munthu wina adadza kuchokera
ku malire a mzinda ali kuthamanga. Iye adati, "Mose!
Anthu ndi mafumu ali kuchita upo woti akuphe iwe. Tuluka
mu mzindawu. Ine ndili kukulangiza iwe mwachoonadi."
21. Iye adachoka ku Aiguputo mwamantha, ali kuyembekeza
kuti zoipa zim'peza. Anali akunena kuti, "Ambuye,
ndipulumutseni ku anthu oipa."
22. Ndipo pamene anali kuyandikira ku Midiyani
Iye adati, "Ambuye anditsogolera ku njira yoyenera."
23. Ndipo pamene adafika pa chitsime cha ku Midiyani,

iye adapeza gulu la anthu aamuna amene adali kumwetsa
ziweto zawo. Ndipo kuonjezera paiwo, padali akazi awiri
amene anali kungosunga nkhosa zawo. Mose adati, "Kodi
vuto lanu ndi chiyani?" Iwo adati, "Sitingathe kumwetsa
nkhosa zathu pokhapokha abusa awa atachotsa ziweto
zawo. Ndipo bambo wathu ndi munthu wokalamba."
24. Mose adawamwetsera nkhosa zawo ndipo adachoka ndi
kukakhala pa m'thunzi nati, "Ambuye, ine ndili kusowa
zabwino zimene munganditumize." 25. Mmodzi mwa
akazi aja adadza kwa iye akuyenda mwamanyazi nati,
"Abambo anga ali kukuitanani kuti akakulipireni chifukwa
chomwetsera ziweto zathu." Ndipo pamene Mose adadza
kwa iwo, adafotokoza nkhani yake kwa iye. Bambo uja
adati, "Usaope. Tsopano wapulumuka m'manja mwa anthu
oipa." 26. Mmodzi mwa akazi aja adati, "Atate, mulembeni
ntchito munthu uyu. Munthu wabwino kumulemba ntchito
ndi amene ali ndi mphamvu ndiponso wokhulupirika."
27. Atate adati, "Ine ndidzakupatsa mmodzi wa ana anga
aakazi kuti umukwatire ngati ungakhale zaka zisanu ndi
zitatu uli kundigwirira ntchito. Koma ngati ufuna ukhoza
kugwira ntchito zaka khumi. Ine sindifuna kukuzunza ayi.
Ngati Mulungu afuna, udzaona kuti ine ndine munthu
wangwiro." 28. Mose adati, "Zimenezi zikhale pakati pa inu
ndi ine. Mwa nthawi ziwirizi ine ndidzakwaniritsa ndipo
pasadzakhale cholakwa kwa ine. Ndipo Mulungu ndi
mboni pa zimene tili kukambiranazi."

29. Ndipo pamene adamaliza nthawi yake, iye anali kupita
ndi mkazi wake. Mose adaona moto kuonjezera pa phiri
la Sinai. Iye adati kwa mkazi wake, "Khala pano chifukwa
ndili kuona moto. Mwina mwake ndikhoza kubweretsa

kuchokera kumeneko nkhani kapena mwatso woyaka
umene ukhoza kuotha.” 30. Ndipo pamene adafika pamalo
paja, iye adaitanidwa kuchokera kumbali ya manja ya chigwa
pa malo odalitsika kuchokera mumtengo. “Oh iwe Mose!
Ndithudi, Ine ndine Mulungu, Ambuye wa zolengedwa
zonse.” 31. “Ndipo ponya pansi ndodo yako.” Ndipo pamene
adaona ndodo yake ili kuyenda ngati njoka, adatembenuka
nathawa osabwevukanso. “Iwe Mose! Bwerera ndipo
usaope. Iwe ndiwe mmodzi wa anthu otetezedwa.” 32. “Ika
dzanja lako m’thumba, ndipo ilo lidzakhala loyera kwambiri
lopanda chilema ndipo ika dzanja lako pamtima pako kuti
uchoke mantha. Kotero zimenezi ndi zizindikiro ziwiri za
Ambuye wako kwa Farao ndi mafumu ake. Mosakaika iwo
ndi anthu osakhulupirira.”
33. Mose adati, “Ambuye wanga! Ine ndidapha mmodzi
mwa anthu awo ndipo ndili ndi mantha kuti mwina akhoza
kukandipha.” 34. “Ndipo Aroni, m’bale wanga, amayankhula
bwino kuposa ine. Mutumizeni iye pamodzi ndi ine
kuti akhoza kukandithandiza kuti akandiyankhulire.
Ndithudi ine ndiopa kuti akandikana.” 35. Iye adati, “Ife
tidzakuonjezera mphamvu pokhala ndi m’bale wako
ndipo ndiika pa inu awiri umboni ndipo iwo sadzatha
kukupwetekani inu chifukwa cha zizindikiro zathu. Inu
pamodzi ndi onse amene amakutsatirani mudzapambana.”
36. Ndipo pamene Mose adadza kwa iwo ndi zizindikiro
zathu zooneka, iwo adati, “Izi si zina ayi koma matsenga
ongopeka ndiponso ife sitidamvepo kuti za mtundu
uwu zinachitikapo kuchokera kwa makolo athu akale.”
37. Ndipo Mose adati, “Ambuye wanga amadziwa
bwinobwino munthu amene amabweretsa chilangizo

chochokera kwa Iye, ndiponso kwa amene tsogolo lake
ndi labwino. Ndithudi anthu onse ochimwa sadzapambana
ayi.” 38. Farawo adati, “Oh inu mafumu! Inu mulibe mulungu
wina amene ine ndimudziwa kupatula ine ndekha. Haman,
ndipangireni ine njerwa zadothi ndipo mundimangire
nyumba yaitali, yonga nsanja, kuti ndikwerepo kupita kwa
Mulungu wa Mose. Ndithudi ine ndili kumuganizira kuti
Mose ndi mmodzi mwa anthu abodza.”

39. Farawo ndi Asirikali ake adadzikweza kwambiri
mu dziko la Aiguputo popanda chifukwa ndipo iwo
anali kuganiza kuti sadzabwereranso kwa Ife. 40. Ndipo
tidamutenga iye pamodzi ndi asirikali ake ndipo
tidawamiza m’nyanja. Ganiza chimene amaona anthu
ochita zoipa. 41. Ife tidawapanga iwo kukhala atsogoleri
oitana anthu kuti apite kumoto koma pa tsiku la kuuka
kwa akufa, palibe mmodzi amene adzawathandiza iwo.
42. Ife tidawatsatira ndi matemberero m’dziko lino ndipo pa
tsiku la kuuka kwa akufa iwo adzakhala anthu onyozeka.
43. Ndipo ife tidaononga mibadwo yoyamba yakale ndipo
tidamupatsa Mose Buku la Chipangano Chakale monga
nyali, langizo ndi chifundo kwa anthu kuti mwina akhoza
kuchenjezedwa.

44. Iwe kudalibe, ku mbali ya kumadzulo kwa phiri,
pamene Ife tinali kumupatsa Mose udindo wake ndiponso
iwe kunalibe pa mwambowu. 45. Koma Ife tidalenga
mibadwo yambiri Mose atafa kale imene inali ndi moyo
wautali. Iwe siunakhale pakati pa anthu a ku Midiyani ndi
kumawalakatulira chivumbulutso chathu. Koma Ife ndi
amene timatumiza Atumwi. 46. Ndipo iwe kudalibe m’mbali
mwa phiri la Sinai pamene tidamuitana Mose. Koma adali

madalitso ochokera kwa Ambuye wako kuti ukachenjeze
mtundu wa anthu umene unalipo iwe usanadze kotero
kuti akhoza kuchenjezedwa. 47. Tikanapanda kukutumiza
iwe ndipo mazunzo akadawagwera chifukwa cha ntchito
zawo zoipa, iwo akadati, "Ambuye, chifukwa chiyani
simudatitumizire Mtumwi kotero kuti tikadatsatira mawu
anu ndiponso tikadakhala okhulupirira." 48. Ndipo pamene
choonadi chadza kwa iwo kuchokera kwa Ife, iwo ali
kufunsa kuti, "Kodi ndi chifukwa chiyani iye sadapatsidwe
monga zomwe zidapatsidwa kwa Mose?" Kodi iwo
sadakane zimene zidapatsidwa kwa Mose kale? Iwo
amati, "Zizindikiro ziwiri za matsenga zili zothandizana."
Ndiponso amanena, "Ife sitidzakhulupirira mu china
chilichonse cha zimenezi."
49. Nena, "Bweretsani Buku lochokera kwa Mulungu
limene lili ndi langizo labwino kuposa malangizo awa ndipo
ine ndidzatsatira ngati zimene muli kunena ndi zoona."
50. Ngati iwo akanika kukuyankha, dziwa kuti iwo ali
kutsatira zilakolako zawo. Kodi ndani amene ali wolakwa
kwambiri kuposa munthu amene amatsatira zilakolako
zake opanda langizo la Mulungu? Ndithudi Mulungu
satsogolera anthu olakwa. 51. Ndithudi tatumiza mawu athu
motsatana kwa iwo kuti akhoze kuchenjezedwa.
52. Iwo amene kale tidawapatsa Buku lino lisadadze,
amakhulupirira mwa ilo. 53. Pamene limalakatulidwa kwa
iwo, amati iwowo "Ife tili kulikhulupirira Bukuli chifukwa
ndi choonadi chochokera kwa Ambuye wathu. Ife
tidadzipereka kwathunthu kalekale mawu awa asadadze."
54. Anthu awa mphotho yawo idzaperekedwa kwa iwo kawiri
chifukwa iwo adapirira ndipo amagonjetsa choipa pochita

chabwino ndi kumapereka gawo la chaulere pa katundu
amene tidawapatsa. 55. Ndipo iwo akamva mawu oipa,
salabadira zonenazo koma amati, “Ife tili ndi ntchito zathu
ndipo nanunso muli ndi ntchito zanu. Mtendere ukhale
kwa inu. Ife sitifuna kugwirizana ndi anthu osadziwa.”
56. Iwe siungamutsogolere aliyense amene umufuna. Ndi
Mulungu yekha amene amatsogolera aliyense amene Iye
wamufuna. Iye amadziwa bwino anthu amene ali oyenera.
57. Iwo amati, “Ngati ife titsatira chilangizo chako, ife
tikuopa kulandidwa dziko lathu.” Kodi Ife sitidawakhazikire
malo otetezedwa kumene zipatso za mtundu uliwonse
zimaperekedwa ngati chakudya kuchokera kwa Ife?
Ndithudi ambiri a iwo ndi anthu osadziwa.
58. Kodi ndi mizinda ingati imene tidaononga imene idali
kunyada chifukwa cha chuma chake? Kotero zimenezi
ndizo nyumba zawo zimene sadakhalitsemo ndipo
tsopano eni ake ndife. 59. Ndipo Ambuye wako sadaononge
mizinda mpaka pamene Iye adadzutsa kuchokera mu iyo,
Mtumwi amene amalalikira za chivumbulutso chathu
ndipo Ife sitidzaononga mzinda pokhapokha anthu okhala
mmenemo ali olakwa.
60. Zinthu zimene mwapatsidwa si zina koma chakudya
ndiponso chionetsero chopanda pake cha m’moyo uno.
Koma chimene chili ndi Mulungu ndicho chabwino
ndiponso chokhalitsa. Kodi simungathe kuzindikira?
61. Kodi anthu awiriwa ndi ofanana? Iye amene tamulonjeza
lonjezo labwino ndipo adzalikwaniritsa ndi iye amene
tamupatsa zokoma zambiri za m’moyo uno koma pa tsiku
lachiweruzo adzakhala m’gulu la iwo olangidwa?
62. Pa tsiku limeneli Mulungu adzawaitana ndipo adzati,

“Kodi aja munkati ndi anzanga ali kuti?” 63. Iwo amene
adzapezeka ndi mlandu wotere adzati, “Awa ndiwo
anthu amene ife tidawasocheretsa. Ife tidawasocheretsa
chifukwa nafenso tidali osochera. Ife tsopano tadzipatula
(kuchoka mwa iwo) ndi kudza kwa inu. Si ndife amene iwo
anali kupembedza.”
64. Ndipo kudzanenedwa kwa iwo kuti, “Itanani
anzanu kuti akuthandizeni.” Iwo adzawaitana koma iwo
sadzawamva ayi. Ndipo iwo adzalawa chilango chowawa.
Iwo adzafunitsitsa akadatsogozedwa bwino. 65. Tsiku
limene Mulungu adzawaitana nati, “Kodi inu mudanena
zotani kwa Mtumwi?” 66. Zodandaula zawo sizidzamveka
ayi, kotero sadzatha kufunsana wina ndi mnzake.
67. Akakhala iye amene alapa zoipa zake nakhulupirira
ndipo achita ntchito zabwino, mwina akhoza kudzakhala
pakati pa anthu opambana.
68. Ndipo Ambuye wako amalenga ndi kusankha aliyense
amene Iye wamufuna. Kusankha si kwawo ayi. Ulemerero
ukhale kwa Mulungu ndipo Iye atalikirane ndi zimene
amamufanizira nazo. 69. Ambuye wako amadziwa zonse
zimene amazibisa m’mitima mwawo ndiponso zimene
amaziulula. 70. Iye ndi Mulungu ndipo palibenso mulungu
wina koma Iye yekha. Kuyamikidwa konse ndi kwake
m’moyo uno ndiponso m’moyo umene uli nkudza. Ndipo
chake ndi chiweruzo ndipo kwa Iye mudzabwerera.
71. Nena, “Ndiuzeni! Ngati Mulungu atapanga usiku
kuti usache mpaka pa tsiku louka kwa akufa, kodi
ndi mulungu uti kupatula Mulungu weniweni amene
akhoza kukupatsani usana? Kodi simukumva?” 72. Nena,
“Ndiuzeni! Ngati Mulungu atapanga usana kuti kusade

mpaka pa tsiku louka kwa akufa, kodi ndi mulungu uti kupatula Mulungu weniweni amene akhoza kukupatsani usiku umene inu mumapumulamo? Kodi inu simukuona?”
73. Mwachifundo chake wakupatsani usiku ndi usana kuti muzipezamo mpumulo ndi kufunafuna chisomo chake ndi kuti muzithokoza.

74. Ndipo pa tsiku limene adzawaitana iwo nati, “Kodi ali kuti iwo amene mumaganiza kuti ndi anzanga?” 75. Ndipo
nthawi yomweyo tidzaitana mboni kuchokera ku mtundu uliwonse ndipo tidzati, “Bweretsani umboni wanu.” Nthawi imeneyo adzadziwa kuti mwini wake choonadi ndi Mulungu ndipo zonse zimene amapeka zidzawathawira.

76. Ndithudi Karuni, mosakayika, adali wa ku mtundu wa Mose. Koma iye amawanyoza iwo chifukwa Ife tidamupatsa nkhokwe za chuma zimene ndithudi makiyi ake samatheka kunyamulidwa ndi anthu angapo a mphamvu. Anthu ake adati kwa iye, “Usadzikundikire chifukwa Mulungu sakonda anthu odzikundikira chifukwa cha chuma.”
77. “Koma ufunefune, kudzera m’zimene Mulungu wakupatsa iwe, kuti upeze moyo umene uli nkudza, ndiponso usaiwale udindo wako m’dziko lino. Khala wabwino monga Mulungu wakuonetsera ubwino wake. Ndipo usalimbike pochita zoipa padziko lapansi chifukwa Mulungu sakonda anthu ochita zoipa.”

78. Iye adati, “Chuma ichi chidapatsidwa kwa ine chifukwa cha nzeru zanga.” Kodi iye sadadziwe kuti Mulungu adaononga m’badwo wonse wa anthu amene adali ndi mphamvu zambiri ndiponso olemera kwambiri iye asanabadwe? Anthu ochita zoipa sadzafunsidwa za machimo awo.

79. Kotero iye adapita kwa anthu ake monyadira atavala
bwino. Anthu amene adali kukonda moyo wa pa dziko
lapansi adati, “Tikadakhala kuti tidali nazo ngati zinthu
zimene zili ndi Karuni! Ndithudi iye ndi wolemera
kwambiri.” 80. Koma iye amene adapatsidwa nzeru adati:
“Tsoka kwa inu! Mphotho ya Mulungu m’moyo umene
uli nkudza ndi yabwino kwa iwo amene amakhulupirira
ndipo amachita zabwino.” Koma mphothoyo palibe amene
adzailandira kupatula okhawo amene amapirira.
81. Kotero Ife tidalamulira nthaka kuti imumeze
Karuni pamodzi ndi chuma chake ndipo sadapeze
wina womuthandiza kwa Mulungu ndipo iye sadathe
kudziteteza. 82. Ndipo iwo amene anali kukhumbira chuma
chake chadzulo adayamba kunena kuti, “Taonani! Mulungu
amapereka moolowa manja kwa aliyense amene wamufuna
ndi monyalapsa kwa aliyense amene Iye wamufuna.
Akadakhala kuti sadatilangize ife chisoni chake, Iye
akadalamulira nthaka kuti itimeze. Taonani! anthu okana
Mulungu sadzakhala opambana ngakhale pang’ono.”
83. Kunena za m’moyo umene uli nkudza, udzakhala wa
iwo amene sadzikweza pa dziko lapansi kapena kuchita
zoipa. Ndipo mapeto abwino ndi a iwo amene ali angwiro.
84. Aliyense amene achita zabwino adzalipidwa zochuluka.
Koma iye amene achita zoipa ndiponso iwo amene achita
ntchito zoipa adzangolipidwa molingana ndi zimene anali
kuchita.
85. Ndithudi Iye amene adalamulira Buku la Korani
kuti livumbulutsidwe kwa iwe adzakubwezera kumalo
komwe udzapite. Nena, “Ambuye wanga adziwa bwino iye
amene amabweretsa langizo loonadi ndiponso iye amene

ndi wosochera.” 86. Ndipo iwe siumayembekezera kuti Buku lolemekezeka lidzavumbulitsidwa kwa iwe koma ndi chifundo chochokera kwa Ambuye wako. Kotero usavomereze zochita za anthu omwe ali osakhulupirira. 87. Usalole wina aliyense kuti akubweze ku chivumbulutso cha Mulungu pamene chavumbulutsidwa kwa iwe ndipo aitane anthu kuti adze kwa Ambuye wako ndipo usakhale m'gulu la anthu amene amaphatikiza milungu ina ndi Mulungu weniweni. 88. Ndipo usamphatikize mulungu wina ndi Mulungu weniweni. Kulibe mulungu wina koma Iye yekha. Zinthu zonse ndi zakutha kupatula Iye yekha. Chake ndi chiweruzo ndipo kwa Iye ndi kumene mudzabwerera.

Sura 29 • Al- Ankabût

## Ankabut

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha.

1. *Alif. Lam Mim.*

2. Kodi anthu amaganiza kuti adzasiyidwa okha osayesedwa chifukwa anena kuti, “Ife ndife okhulupirira?” 3. Ndipo ndithudi Ife tidawayesa anthu amene adalipo iwo asanadze. Ndithudi Mulungu adzawazindikira iwo amene ndi olungama, ndipo ndithudi, adzawazindikira iwo amene ndi abodza.

4. Kodi kapena iwo amene amachita zoipa amaganiza kuti adzatithawa ife? Iwo amaweruza molakwa.

5. Aliyense amene amakhulupirira kuti adzakumana ndi
Mulungu nthawi imene Mulungu adakhazikitsa, ndithudi,
idzabwera ndipo Iye ndi wakumva ndi wodziwa. 6. Ndipo
aliyense amene adzipereka kwathunthu, akudzipereka
podzithandiza iye mwini. Ndithudi Mulungu ndi woima
payekha ndipo Iye safuna thandizo lochokera kwa
zolengedwa zake. 7. Ndipo iwo amene amakhulupirira
ndipo amachita ntchito zabwino, Ife tidzawakhululukira
machimo awo ndikuwapatsa malipiro ofanana ndi ntchito
zawo zabwino.
8. Ndipo Ife tidamulamula munthu kuonetsa ubwino kwa
makolo ake koma ngati iwo akuuza kuti uzindiphatikiza
Ine ndi ena ake amene iwe siuwazindikira, usawamvere
ayi. Kwa Ine ndiko mudzabwerera ndipo ndidzakuuzani
zimene munali kuchita. 9. Ndipo iwo amene akhulupirira
ndi kumachita ntchito zabwino, ndithudi, Ife tidzawaika
m'gulu la anthu angwiro.
10. Ndipo pakati pa anthu pali iye amene amati, "Ife
timakhulupirira mwa Mulungu." Koma akangoona
mavuto chifukwa chodzipereka kwa Mulungu, amaganiza
kuti kuponderezedwa kwawo ndi anthu ndi mkwiyo
wochokera kwa Mulungu! Ndipo ngati thandizo lidza kwa
iwe kuchokera kwa Ambuye wako, ndithudi, iwo adzati,
"Ife tidali kumbali yako." Kodi mukuganiza kuti Mulungu
sadziwa zonse zimene zili m'mitima mwawo pakati pa
zolengedwa zake zonse? 11. Ndithudi Mulungu amawadziwa
anthu onse okhulupirira ndi anthu onse a chinyengo.
12. Ndipo anthu osakhulupirira amanena kwa anthu
okhulupirira kuti, "Tsatirani njira yathu ndipo ife
tidzavomera chilango chifukwa cha kuchimwa kwanu. Iwo

sadzavomera chilango china chilichonse m'malo mwawo. Ndithudi iwo ndi abodza. 13. Iwo adzanyamula mtolo wawo pamodzi ndi mitolo ina ndi yawo. Ndipo patsiku lachiweruzo iwo adzafunsidwa kufotokoza mabodza awo.

14. Ndipo ndithudi tidamutumiza Nowa kwa anthu ake ndipo adakhala pakati pawo zaka chikwi chimodzi kuchotsapo zaka makumi asanu. Ndipo chigumula chidawapeza ali pa uchimo. 15. Kotero tidamupulumutsa iye pamodzi ndi iwo amene adali naye m'chombo ndipo tidachipanga icho kukhala phunziro kwa anthu a mitundu yonse.

16. Ndipo Ife tidamupulumutsa Abrahamu pamene adati kwa anthu ake, "Pembedzani Mulungu ndipo muzimuopa Iye. Chimenecho chidzakhala chinthu chabwino kwa inu ngati mukadazindikira." 17. Chifukwa inu mumapembedza mafano oonjezera pa Mulungu ndipo inu mumapeka bodza. Zinthu zimene mumapembedza zoonjezera pa Mulungu zilibe mphamvu zokupatsani zofuna zanu. Kotero pemphani zofuna zanu kwa Mulungu ndipo muzimuthokoza Iye. Kwa Iye ndiko kumene mudzabwerera. 18. Ndipo ngati inu mukana uthenga dziwani kuti nawonso amene adalipo inu musanadze adachita chimodzimodzi. Ndipo udindo wa Mtumwi ndi kulalikira pagulu momveka.

19. Iwo sakuona mmene Mulungu amayambitsira chilengedwe ndiponso mmene amachibwerezanso. Ndithudi zimenezo ndi za pafupi kwa Mulungu. 20. Nena, "Yendani paliponse pa dziko lapansi ndipo muone mmene Mulungu adayambitsira chilengedwe. Kotero Mulungu adzalenga chilengedwe chinanso. Mulungu ali ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse." 21. Iye amalanga

aliyense amene wamufuna ndiponso amaonetsa chifundo
chake kwa aliyense amene wamufuna. Ndipo ndi kwa Iye
kumene nonse mudzabwerera. 22. Kaya ndi pa dziko lapansi
kapena kumwamba, kulibe kumene inu mungathawire.
Ndipo inu mulibe wina kupatula Mulungu amene
angakutetezeni kapena kukuthandizani. 23. Onse amene
amakana zizindikiro za Mulungu ndiponso zokumana
naye m'moyo umene uli nkudza ndiwo amene amakayika
za chifundo changa. Ndipo iwo adzalandira chilango
chowawa kwambiri.

24. Yankho la anthu a Abrahamu lidali lamwano ndipo
adati, "Mumuphe kapena mumutenthe." Koma Mulungu
adamupulumutsa iye ku moto. Ndithudi mu zimenezi muli
phunziro kwa anthu okhulupirira. 25. Ndipo iye adati, "Inu
mwasankha kupembedza mafano kuonjezera pa Mulungu
weniweni chifukwa chokweza mgwirizano wa pakati panu
m'moyo uno. Koma pa tsiku lachiweruzo inu mudzakanana
wina ndi mnzake. Ndipo malo anu akakhala ku moto ndipo
inu simudzakhala ndi wina wokuthandizani." 26. Koma Loti
adamukhulupirira iye. Iye adati, "Ndidzachoka pa nyumba
yanga chifukwa cha Ambuye wanga chifukwa Iye ndi
wamphamvu zambiri ndi wanzeru." 27. Ndipo tidamupatsa
Abrahamu, Isake ndi Yakobo ndipo tidakhazikitsa pakati pa
ana ake utumiki ndi chivumbulutso. Ndipo Ife tidamupatsa
mphotho yake m'moyo uno ndipo iye adzakhala m'moyo
umene uli nkudza, pagulu la anthu olungama.

28. Ndipo tidatumiza Loti, kotero iye adati kwa
anthu ake, "Inu muli kuchita zinthu zonyansa zimene
sizidachitikeponso ndi mtundu wa anthu kuyambira
kalekale." 29. "Kodi inu mumakaputa anthu a aamuna ndi

kuchita chifwamba m'misewu ndiponso mumaphunzitsa
zoipa ngakhale m'magulu anu?" Iwo sadayankhe china
chilichonse kupatula kuti iwo adati, "Bweretsa pa ife
chilango cha Mulungu ngati iwe ukunena zoona." 30. Iye
adati, "Ambuye wanga! Thandizeni polimbana ndi anthu
oipawa."

31. Ndipo pamene Atumwi athu adadza kwa Abrahamu,
ndi nkhani ya bwino, iwo adati, "Ndithudi ife tidzaononga
anthu a mu mzinda uno chifukwa anthu ake ndi
osalungama." 32. Iye adati, "Ndithudi mu mzindamo muli
Loti." Iwo adati, "Ife tikudziwa amene ali m'menemo.
Ndithudi ife tidzamupulumutsa iye ndi omutsatira ake
onse kupatula mkazi wake. Iye adzakhala m'gulu la anthu
otsalira." 33. Ndipo pamene Atumwi athu adadza kwa Loti,
iye anada nkhawa pa zimene zingawachitikire iwo ndipo
iye adaoneka wopanda mphamvu yowateteza iwo. Ndipo
iwo adati, "Usaope kapena kuda nkhawa. Ndithudi ife
tidzakupulumutsa iwe pamodzi ndi okutsatira ako kupatula
mkazi wako. Iye adzakhala m'gulu la anthu otsalira."
34. Ndithudi Ife tidzatsitsa chilango kuchokera kumwamba,
kuti chilange anthu a mzinda uno chifukwa cha machimo
awo. 35. Ndithudi Ife tasiya chiphunzitso chokwanira kwa
anthu ozindikira.

36. Ndipo kwa anthu a ku Midiyani tidatumiza m'bale
wawo Shaibu ndipo iye adati, "Oh anthu anga! Tumikirani
Mulungu ndipo opani tsiku limene lili nkudza ndipo
musayambitse chisokonezo m'dziko pochita zinthu zoipa."
37. Koma iwo adamukana iye, kotero chivomezi chachikulu
chidadza pa iwo ndipo mitembo yawo idali lambilambi
m'nyumba zawo.

38. Ndi Aad ndi Thamoud. Chitsimikizo chake chili
m'mabanja a m'mizindayi. Satana adawapangitsa kuganiza
kuti ntchito zawo zoipa zidali zabwino ndipo iye
adawabweza ku njira yoyenera ngakhale kuti iwo adali
anthu anzeru ndi aluntha.
39. Ndipo Ife tidaononga Karuni, Farawo ndi Hamani.
Ndithudi Mose adadza kwa iwo ndi chiphunzitso chabwino
koma iwo anali kukhala mwamwano m'dziko ngakhale
kuti iwo sakadatha kutigonjetsa Ife. 40. Kotero tidalanga
aliyense chifukwa cha machimo ake. Pakati pa iwo padali
iwo amene tidawatumizira mvula yamkuntho, ndipo pakati
pawo padali iwo amene adavutika ndi mphenzi, ndipo
pakati pawo padalinso iwo amene adamezedwa ndi nthaka
ndipo padalinso iwo amene tidawamiza ndipo Mulungu
sadalakwe ayi koma iwo ndiwo amene adalakwira mizimu
yawo.
41. Fanizo la iwo amene amasankha owateteza kuonjezera
pa Mulungu ndi Kangaude amene amamanga nyumba yake
yaulusi. Ndipo ndithudi iwo akadayenera kudziwa kuti
nyumba ya Kangaude ndi imodzi mwa nyumba zosalimba.
42. Ndithudi Mulungu amadziwa chilichonse chimene
iwo amapembedza kuonjezera pa Iye ndipo Iye ndi
wamphamvu ndi wanzeru. 43. Ndipo zitsanzozi tili kuziulula
chifukwa cha anthu koma palibe amene amazizindikira
koma ophunzira okha. 44. Mulungu adalenga kumwamba
ndi dziko lapansi mwachoonadi. Ndithudi muli phunziro
mu zimenezi kwa anthu okhulupirira.
45. Lakatula zimene zavumbulutsidwa kwa iwe kuchokera
m'Buku ndipo pitiriza kupemphera. Ndithudi mapemphero
amateteza munthu ku machimo ndi zinthu zoipa. Ndithudi

kukumbukira Mulungu ndi chinthu chachikulu ndipo
Mulungu amadziwa zonse zimene mumachita.
46. Ndipo musatsutsane ndi anthu okhulupirira za
m'Buku pokhapokha kutakhala koyenera kutero, kupatula
okhawo amene amachita zoipa. Nena, "Ife timakhulupirira
mu izo zimene zavumbulutsidwa kwa ife ndi zimene
zidavumbulutsidwa kwa inu ndipo Mulungu wathu ndi
Mulungu wanu ndi mmodzi ndipo ife tadzipereka kwa Iye."
47. Ndipo kotero Ife tavumbulutsa Buku lolemekezeka kwa
iwe. Kotero onse amene tawapatsa Buku amakhulupirira
mwa ilo ndipo palibe amene amakana chivumbulutso
chathu kupatula anthu osalungama. 48. Ndipo iwe
siudalakatule za m'Buku lina ili lisanadze. Ndipo iwe
siudalembe Buku lina lililonse ndi manja ako. Zikadatero,
ndithudi, anthu oyankhula zachabechabe akadakayika.
49. Iyayi! Izi ndi ziphunzitso zomveka zimene zili m'mitima
ya iwo amene adapatsidwa nzeru ndipo palibe amene
amakana chiphunzitso chathu kupatula wosalungama.
50. Iwo amati, "Bwanji Ambuye wake sadamupatse
zizindikiro?" Nena, " Zizindikiro zonse zili ndi Mulungu
ndipo ine ndine mchenjezi chabe." 51. Kodi sizidakwanire
kuti tavumbulutsa Buku lolemekezeka kwa iwe limene lili
kuwerengedwa kwa iwo? Ndithudi m'Bukuli muli chifundo
ndi chikumbutso kwa anthu okhulupirira. 52. Nena,
"Mulungu ndi mboni yokwana pakati pa ine ndi inu. Iye
amadziwa chimene chili kumwamba ndi pa dziko lapansi."
Ndipo iwo amene amakhulupirira zabodza, ndiponso
sakhulupirira mwa Mulungu, amenewa, ndi anthu olephera.
53. Iwo amakukakamiza kuti ubweretse chilango msanga.
Ndipo zikadakhala kuti nthawi yake siidakhazikitsidwe

kale, ndithudi, chilango chikadakhala chitadza kale pa iwo. Ndithudi icho chidzadza pa iwo mwadzidzidzi pamene iwo sali kuchiganizira. 54. Iwo ali kukukakamiza kuti ubweretse chilango. Ndithudi Gahena idzadzadza ndi anthu osakhulupirira. 55. Patsiku limene chilango chidzadza pa iwo kuchokera kumwamba ndi padziko lapansi mawu adzati, “Lawani inu zipatso za ntchito zanu.”

56. Oh inu akapolo anga amene mwakhulupirira! Ndithudi dziko langa lili ndi malo ambiri. Kotero ndipembedzeni Ine ndekha. 57. Mzimu uliwonse udzalawa imfa. Pomaliza nonse mudzabwerera kwa Ife. 58. Ndipo iwo amene amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino, otere tidzawapatsa malo kumwamba amene pansi pake pamayenda mitsinje kuti akhale m’menemo mpaka kale kale. Eti kukoma mphotho ya iwo amene amachita zabwino. 59. Iwo amapirira ndipo amaika chikhulupiriro chawo mwa Ambuye wawo ndi Mtetezi wawo. 60. Kodi zilipo zolengedwa zingati zimene sizisunga chakudya chawo? Ndi Mulungu amene amazidyetsa izo pamodzi ndi inu nomwe. Ndipo Iye ndi wakumva ndi wodziwa.

61. Ndithudi ngati iwe utawafunsa kuti kodi ndani amene adalenga kumwamba ndi dziko lapansi ndiponso amene adalamula dzuwa ndi mwezi kumvera malamulo ake? Ndithudi iwo adzayankha kuti ndi Mulungu. Nanga ndi chifukwa chiyani iwo amakana choonadi? 62. Mulungu amapereka moolowa manja kwa aliyense amene Iye wamufuna ndipo amamana aliyense amene Iye wamufuna. Ndithudi Mulungu amadziwa chinthu china chilichonse. 63. Ngati iwe ungawafunse kuti kodi ndani amene amagwetsa mvula ndipo amapereka moyo ku nthaka

imene idali ya kufa? Ndithudi iwo adzayankha kuti, “Ndi Mulungu.” Nena “Kuyamikidwa konse kukhale kwa Iye.” Iyayi, ambiri a iwo sazindikira.

64. Ndipo moyo wa padziko lapansi siuli kanthu koma masewera ndi kongotayira nthawi. Ukakhala moyo umene uli nkudza, umenewo ndiwo weniweni, iwo akadadziwa!
65. Kotero iwo akamakwera zombo amapempha kwa Mulungu modzipereka ndi modzichepetsa. Koma Iye akawafikitsa pa mtunda mwaubwino, Ah! iwo amamufanizira Iye ndi zina zake. 66. Kotero iwo amaonetsa kusathokoza pa zimene tawapatsa kuti akhoza kusangalala; ndipo iwo adzazindikira posachedwapa.

67. Kodi iwo saona kuti tateteza malo odalitsika pamene anthu ena ali kutengedwa mwankhanza pa malo owazungulira? Kodi iwo adzakhala ali kukhulupirirabe zabodza ndi kukana ubwino wa Mulungu? 68. Kodi woipitsitsa ndani kuposa munthu amene amapeka bodza lokhudza Mulungu kapena amene amati choonadi ndi chabodza pamene auzidwa za icho? Kodi Gahena siidzakhala malo okhalamo anthu onse osakhulupirira?
69. Akakhala iwo amene amalimbikira kugwira ntchito yathu,ndithudi, Ife tidzawatsogolera ku njira zathu. Ndithudi Mulungu amakhala ndi iwo amene amachita zabwino.

# AL RUM

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni chosatha.

1. *Alif Lam Mim.*

2. Aroma agonjetsedwa, 3. M'dziko loyandikana nalo ndipo
iwo atagonja, pambuyo pake adzapambana. 4. M'zaka
zowerengeka. Mulungu ndiye Mwini ulamuliro ndipo pa
tsiku limeneli onse okhulupirira adzakondwera. 5. Ndi
chithandizo cha Mulungu. Iye amathandiza aliyense
amene wamufuna. Iye ndi wamphamvu, ndiponso Mwini
chisoni chosatha. 6. Ili ndi lonjezo la Mulungu. Mulungu
saphwanya lonjezo lake ndipo anthu ambiri sadziwa. 7. Iwo
amangodziwa zokhazo zimene amaziona za m'moyo uno
koma za m'moyo umene uli nkudza, iwo safuna kumva
china chilichonse cha izo.
8. Kodi iwo saganizira pa okha kuti Mulungu adalenga
kumwamba ndi dziko lapansi ndi zinthu zonse zimene
zikhala m'menemo mwachoonadi ndi mwa kanthawi
yokhazikitsidwa? Ndipo, ndithudi, anthu ambiri amakana
zoti adzakumana ndi Ambuye wawo. 9. Kodi iwo sadayende
pa dziko ndi kuona zimene zidawaonekera anthu amene
adalipo kale? Iwo adali ndi mphamvu zambiri kuposa awa,
ndipo adakumba nthaka ndiponso adamanga pa nthakayo
nyumba zambiri kuposa zimene awa amanga. Ndipo
kudadza kwa iwo Atumwi awo ndi chiphunzitso chomveka
ndipo sikudali koyenera kuti Mulungu awachitire zinthu

zosalungama koma kuti iwo adalakwira mizimu yawo.
10. Choipa chidatsata munthu amene anali kuchita zoipa
chifukwa iwo adakana chiphunzitso cha Mulungu ndipo
anali kuwaseka iwo.
11. Mulungu ndiye amene amalenga zolengedwa ndipo
adzazibwereza ndipo ndi kwa Iye kumene mudzabwerera.
12. Ndipo pa nthawi imene ola lidzadza, anthu onse ochita
zoipa adzakhala ndi nkhawa. 13. Ndipo iwo sadzakhala
ndi ena alionse owathandiza ochokera pakati pa milungu
yawo imene anali kupembedza kuonjezera pa Mulungu
weniweni ndipo iwo adzakhala okana milungu yawo.
14. Ndipo pa nthawi imene ola lidzadza, pa nthawi imeneyi,
iwo adzasiyanitsidwa wina ndi mnzake. 15. Ndipo onse
amene adakhulupirira ndipo adachita ntchito zabwino,
iwo adzasangalatsidwa m'munda wa Paradiso. 16. Iwo
amene sadakhulupirire ndipo adakana chiphunzitso
chathu ndi kukumana kwa m'moyo umene uli nkudza, awa
ndiwo amene adzatengedwa kupita ku chilango. 17. Kotero
lemekezani Mulungu pamene mulowa nthawi ya madzulo
ndi pamene mulowa nthawi ya m'mawa. 18. Inde. Kwa Iye
kukhale kuyamikidwa kumwamba ndi padziko lapansi
ndiponso pa nthawi yamasana ndi yamadzulo.
19. Iye ndiye amene amadzutsa anthu kuchokera ku
anthu akufa ndipo amadzutsa anthu akufa kuchokera ku
anthu amoyo ndiponso amapereka moyo ku nthaka ikafa.
Ndipo mmenemo ndi mmene mudzaukitsidwire. 20. Ndipo
chimodzi cha zizindikiro zake ndi chakuti Iye adakulengani
inu kuchokera ku fumbi, ndipo inu, ndinudi, anthu amene
mudamwazidwa. 21. Ndipo pakati pa zizindikiro china
ndi chakuti Iye adalenga akazi kuchokera mwa inu kuti

mukhoza kupeza mpumulo mwa iwo ndipo adaika pakati
panu chikondi ndi chisoni. Ndithudi muli phunziro muichi
kwa anthu amene amaganiza bwino.
22. Ndipo pakati pa zizindikiro zake ndi kalengedwe ka
kumwamba ndi dziko lapansi ndi kusiyana kwa zilankhulo
zanu ndiponso maonekedwe a makungu anu. Ndithudi mu
chimenechi muli zizindikiro kwa anthu ophunzira. 23. Ndipo
pakati pa zizindikiro zake ndi kugona kumene mumagona
usiku ndi usana kufunafuna chisomo chake. Ndithudi mu
chimenechi muli chizindikiro kwa anthu amene amatha
kumva. 24. Ndipo pakati pa zizindikiro zake ndi chakuti
Iye amakuonetsani mphezi imene imakuchititsani mantha
ndiponso kukupatsani chikhulupiriro. Ndipo amatumiza
mvula kuchokera ku mitambo ndiponso amapereka moyo
ku nthaka ikafa. Ndithudi mu chimenechi muli zizndikiro
kwa anthu ozindikira.
25. Ndipo pakati pa zizindikiro zake ndi chakuti
kumwamba ndi dziko lapansi zimadzichepetsa potsatira
malamulo ake ndipo pamene Iye akuitanani inu kamodzi
kokha kuchokera m'nthaka, Taonani inu mudzadza
mwamsanga msanga. 26. Ndipo chilichonse chimene chili
kumwamba ndi padziko lapansi ndi chake ndipo zonse
zimamumvera Iye. 27. Ndipo Iye ndiye amene amayambitsa
chilengedwe ndipo adzachibwerezanso ndipo zimenezi ndi
zapafupi kwa Iye. Ndipo wake ndi ulemerero kumwamba
ndi padziko lapansi. Ndipo Iye ndiye Mwini mphamvu
zonse ndi Mwini nzeru zonse.
28. Iye ali kupereka chitsanzo chokhudza inu nomwe.
Kodi inu muli nawo akapolo amene amakhala anzanu
pa zinthu zimene takupatsani ndipo kuti mumagawana

nawo zinthuzo mofanana ndiponso mumawaopa iwo
monga momwe mumaoperana? Mmenemo ndi mmene
timasiyanitsira chiphunzitso chathu kwa anthu amene
amazindikira. 29. Iyayi! Onse osalungama amatsatira
zilakolako zawo mosadziwa. Kotero ndani angatsogolere
iye amene Mulungu wamusocheretsa? Ndipo iwo
sadzakhala ndi wowathandiza.
30. Kotero dzipereke kwathunthu ku chipembedzo
choonadi, chipembedzo, chenicheni, chimene
Mulungu adalamula kuti munthu ayenera kutsatira.
Chilengedwe chimene Mulungu adalenga mtundu wa
anthu sichingasinthidwe. Ndithudi pali Mulungu, icho
ndicho chipembedzo choona. Koma ambiri a mtundu wa
anthu sadziwa. 31. Lapani kwa Iye ndiponso muopeni Iye.
Pitirizani kupemphera nthawi zonse ndipo musakhale inu
pakati pa iwo amene amafanizira milungu ina ndi Mulungu
weniweni. 32. Pali anthu amene amagawa chipembedzo
chawo ndi kukhala mipingo yosiyanasiyana ndipo mpingo
uliwonse umasangalala ndi zimene uli nazo.
33. Ndipo pamene mavuto adza pa anthu, iwo amalira kwa
Ambuye wawo ndi kudza kwa Iye modzichepetsa. Koma
pamene Mulungu awaonetsa gawo lachisoni chochokera
kwa Iye Mwini, ena a iwo amayamba kupembedza milungu
ina yoonjezera pa Ambuye wawo. 34. Akhala ngati ali
kuonetsa kusathokoza pa zimene tawachitira. Basangalalani
mwa kanthawi kochepa ndipo posachedwapa mudzadziwa
kupusa kwanu. 35. Kodi kapena Ife tidawatumizira lamulo
limene limanena za zinthu zimene iwo amazipembedza
zoonjezera pa Mulungu ?
36. Ndipo pamene tiwaonetsera anthu chifundo chathu,

iwo amasangalala kwambiri chifukwa cha chifundocho
ndipo ngati choipa chidza pa iwo chifukwa cha zimene iwo
achita ndi manja awo, taonani! Iwo amadandaula kwambiri.
37. Kodi iwo saona kuti Mulungu amapereka moolowa
manja kwa aliyense amene Iye wamufuna ndiponso
zomupatsazochepa munthu yemwe wamufuna. Ndithudi
mu chimenechi muli phunziro kwa anthu okhulupirira.
38. Kotero apatseni zosowa zawo abale anu, anthu osauka
ndi a paulendo. Ichi ndicho chinthu chabwino kwambiri
kwa iwo amene afuna chisangalalo cha Mulungu ndipo
awa ndiwo amene ali opambana. 39. Chimene mumapereka
ngati chiongoladzanja kuti chionjezere chuma cha anthu,
sichidzakhala ndi chionjezero kwa Mulungu. Koma
zopereka zimene mupereka ngati chaulere ndi cholinga
chopeza madalitso a Mulungu ndi chimenechi chimene
chidzaonjezeredwa kwambirimbiri.

40. Ndi Mulungu amene anakulengani inu amene
amakupatsani zofuna zanu. Iye adzakonza kuti mufe
patsogolo pake pano ndipo kenaka adzakupatsaninso moyo.
Kodi chilipo china chilichonse chimene mungachifanizire
ndi chimene chingachite zimenezi? Ulemerero ukhale kwa
Iye ndipo Iye akhale zopambana kuposa zonse zimene
amazifanizira ndi Iye. 41. Zinthu zoipa zalowa m'dziko
ndiponso m'nyanja chifukwa cha ntchito za anthu zimene
amachita ndi manja awo. Mulungu akhoza kuwalawitsa
chilango chifukwa cha ntchito zawo kuti mwina athe
kutembenuka. 42. Nena "Pitani paliponse pa dziko ndi
kuona zimene zidawaonekera anthu amene adalipo kale.
Ambiri a iwo adali opembedza mafano."

43. Kotero dziperekeni kwathunthu ku chipembedzo

choona lisanadze tsiku loopsa kuchokera kwa Mulungu
limene silidzatheka kulizemba. Pa tsiku limeneli
anthu adzagawidwa m'magulu. 44. Onse osakhulupirira
adzalangidwa chifukwa cha kusakhulupirira kwawo ndipo
onse amene amachita ntchito zabwino adzadzisungira
zinthu zabwino kumwamba. 45. Ndipo Iye adzawapatsa
malipiro abwino onse amene amakhulupirira ndipo
amachita ntchito zabwino kuchokera ku zokoma zake.
Ndipo Iye sakonda anthu osakhulupirira.
46. Ndipo chimodzi mwa zizindikiro zake ndi chakuti
amatumiza mphepo imene imabweretsa zabwino ndi
cholinga choti mulawe chisomo chake ndiponso kuti
zombo ziyende mwamalamulo ake ndiponso kuti
inu muzifunafuna chifundo chake ndi kumuthokoza.
47. Ndithudi Ife tidatumiza, Atumwi kwa anthu awo iwe
usanabadwe ndipo iwo adadza kwa iwo ndi chiphunzitso
choyenera. Ife tidapereka chilango kwa anthu ochimwa
ndipo kuthandiza anthu okhulupirira ndi udindo wosatha
kwa Ife.
48. Mulungu ndiye amene amatumiza mphepo kuti
iyendetse mtambo ndipo amaumwaza mlengalenga monga
momwe wafunira. Iye amauphwanya ndipo inu mumaona
mvula ili kugwa kuchokera mu mtambowo. Iye amagwetsa
mvula pa akapolo ake amene wawafuna. Taonani! Iwo
amakhala osangalala. 49. Ngakhale kuti, iyo isanadze, iwo
anali kuda nkhawa. 50. Taonani zizindikiro za chisoni cha
Mulungu mmene amaperekera moyo ku nthaka imene
inali yakufa. Ndithudi Iye adzadzutsa zakufa kuti zikhale
zamoyo. Iye ali ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse.
51. Ndipo ngati Ife tikatumiza mphepo imene imapangitsa

mbewu zawo kusanduka za chikasu, iwo amakhala
osathokoza. 52. Ndithudi iwe siungathe kumupanga munthu
wakufa kuti amve ndiponso siungathe kumupanga munthu
wosamva kuti amve kuitana pamene iwo atembenuka ndi
kuthawa. 53. Ndipo iwe siungathe kumutsogolera munthu
wakhungu kuti asiye kulakwa kwake. Palibe amene
adzakumvera kupatula okhawo amene amakhulupirira mu
chiphunzitso chathu.

54. di Mulungu amene adakulengani inu ofoka ndipo
adakupatsani mphamvu pambuyo pa kufoka. Ndipo
atakupatsani mphamvu adakupatsani kufoka ndi imvi.
Iye amalenga chilichonse chimene wafuna ndipo ndiye
amene amadziwa zonse ndipo ndiye Mwini mphamvu.
55. Ndipo pamene ola lidzadza, anthu ochimwa adzalumbira
kuti adangokhala ola limodzi lokha. Kotero iwo amakhala
onamizidwa. 56. Ndipo iwo amene adapatsidwa nzeru ndi
chikhulupiriro adzati, “Ndithudi inu mwakhala molingana
ndi malamulo a Mulungu mpaka pa tsiku louka kwa
akufa. Kotero ili ndilo tsiku louka kwa akufa koma inu
simunalidziwe ayi.” 57. Koma patsiku limeneli zodandaula
zawo sizidzawathandiza anthu onse ochimwa ndipo
sizidzamveka ayi.

58. Ndithudi m’Buku ili la Korani anthu tawaikiramo
zitsanzo zambiri zosiyanasiyana ndipo ngati iwe
utawabweretsera chiphunzitso iwo amene sakhulupirira
adzati, “Iwe siuli kutsatira china chilichonse koma bodza
ndi matsenga.” 59. Mmenemo ndi mmene Mulungu
amatsekera mitima ya anthu osadziwa. 60. Kotero pirirani.
Lonjezo la Mulungu ndi loona ndipo usalole anthu opanda
chikhulupiriro kuti akuderere iwe.

# LUQMAN

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni chosatha.

1. *Alif Lam Mim.*

2. Awa ndi mawu a m'Buku la nzeru, 3. Chilangizo ndi
chifundo kwa anthu angwiro, 4. Amene amapemphera
nthawi zonse, amene amapereka msonkho wothandiza
anthu osauka ndipo amakhulupirira m'moyo umene uli
nkudza. 5. Amenewa ndiwo amene atsogozedwa bwino ndi
Ambuye wawo ndipo ndithudi adzakhala opambana.
6. Koma pakati pa anthu, alipo ena amene amagula
nkhani zopanda pake ndi zopanda tanthauzo ndi cholinga
chosocheretsa anthu ku njira ya Mulungu ndi kuipanga
iyo kukhala chinthu choseketsa. Awa adzalandira chilango
chochititsa manyazi. 7. Ndipo pamene chivumbulutso
chathu chilakatulidwa kwa iye, iye amatembenuka monyada
kuoneka ngati kuti sadamve china chilichonse, kapena
ngati kuti m'makutu mwake muli phula kotero muuzeni
za chilango chowawa. 8. Akakhala iwo amene akhulupirira
ndipo amachita ntchito za bwino, ndithudi, adzakhala ku
Paradiso. 9. Kukhalamo mpaka kalekale ndi lonjezo loona
la Mulungu. Ndipo Iye ndiye Mwini mphamvu ndipo ndi
wanzeru zonse.
10. Iye adalenga kumwamba popanda nsanamira monga
muonera ndipo adalenga mapiri pa dziko lapansi kuti
mwina dziko likhoza kuyenda pamodzi ndi inu. Ndipo

m'dzikomo adaikamo nyama za mtundu uliwonse. Ndipo
ife timatumiza mvula kuchokera ku mtambo ndipo
timameretsa mbewu za mitundu yosiyanasiyana. 11. Ichi ndi
chilengedwe cha Mulungu ndipo ndionetseni zimene iwo
amene amakhala pafupi naye adalenga. Iyayi, anthu opanda
chilungamo ndi olakwa.

12. Ndithudi Ife tidamupatsa nzeru Luqman ponena
kuti, "Thokozani Mulungu. Aliyense amene amathokoza
Mulungu, amathokoza chifukwa cha mzimu wake ndipo
aliyense amene sathokoza, ndithudi, Mulungu sasowa
kanthu ndipo ndi wolemekezeka." 13. Ndi pamene Luqman
adamuuza mwana wake adamulangiza kuti, "Mwana wanga
usamafanizire Mulungu ndi china chilichonse chifukwa ndi
tchimo loopsa."

14. Ndipo Ife timamulamula munthu kuonetsa chifundo
kwa makolo ake. Movutika amayi ake adamubereka iye
ndipo m'zaka ziwiri adamuyamwitsa. Kotero, thokozani
Ine ndiponso thokozani makolo anu chifukwa ndi kwa
Ine kumene mudzabwerera. 15. Koma ngati akuuza kuti
uzindifanizira Ine ndi china chake chimene siuchidziwa,
usawamvere. Aonetsere chifundo ndipo utsatire zochita
za iye amene amalapa kwa Ine ndi kundimvera. Ndipo
kwa Ine ndi kumene nonse mudzabwerera ndiponso
ndidzakuuzani zonse zimene mudachita.

16. "Oh mwana wanga! Choipa ngakhale chitakhala
ngati njere ya mpiru imene idakwiriridwa m'kati mwa
mwala kapena kwina kulikonse kumwamba kapena pa
dziko lapansi, Mulungu adzachitulutsa. Mulungu ali ndi
nzeru ndiponso amadziwa chinthu china chilichonse."
17. "Oh mwana wanga! Limbikira kupemphera, khazikitsa

chilungamo ndipo udziletse kuchita zoipa. Khala opirira
pa chilichonse chimene chidza pa iwe.” Ndithudi! Awa
ndi malamulo ofunika amene adalamula Mulungu ndipo
ayenera kutsatidwa. 18. “Usanyodole anthu kapena kuyenda
modzitukumula pa dziko. Mulungu sakonda anthu
odzitukumula.” 19. “Ndipo uyenera kukhala wofatsa ndipo
mawu ako azikhala otsika chifukwa mawu aukali kwambiri
ndi kulira kwa bulu.”
20. Kodi simuona kuti Mulungu wapanga zinthu zimene
zili kumwamba ndiponso zimene zili padziko lapansi
kukumverani inu ndipo adakupatsani inu zabwino zooneka
ndi zosaoneka ndi maso? Ndipo pakati pa anthu pali iye
amene amatsutsa zinthu zokhudza Mulungu ngakhale iye
sadziwa china chilichonse, kapena chilangizo kapena Buku
lopereka muuni. 21. Ndipo zikanenedwa kwa iwo kuti:
Tsatirani zimene Mulungu wavumbulutsa iwo amati, Iyayi.
Ife sititsatira china chilichonse koma zokhazo zimene
tidapeza makolo athu ali kutsatira. Ngakhale kuti Satana
ali kuwaitanira iwo ku chilango cha moto?
22. Aliyense amene adzipereka kwa Mulungu ndipo
amachita ntchito zabwino, amagwiritsa chotsekulira
chimene chiyenera kugwiridwa ndipo kwa Mulungu
zinthu zonse zidzabwerera. 23. Koma ngati wina akana
kukhulupirira, usalole kuti kusakhulupirira kwakeko kuti
kukumvetse chisoni. Kwa Ife, anthu onse adzabwerera
ndipo tidzawauza zoona za ntchito zawo. Mulungu
amadziwa bwino zonse zimene zili m’mitima mwa anthu.
24. Ife timawalekerera pa kanthawi kochepa ndipo pomaliza
Ife tidzawakankha kupita ku chilango chowawa.
25. Ndipo ngati iwe uwafunsa kuti ndani amene adalenga

kumwamba ndi dziko lapansi, ndithudi, iwo adzati,
“Mulungu.” Nena, “Ulemerero ukhale kwa Mulungu.”
Iyayi! Ambiri a iwo sadziwa. 26. Chilichonse chimene chili
kumwamba ndi pa dziko lapansi ndi cha Mulungu. Ndithudi
Mulungu sasowa chilichonse ndipo ndi woyamikidwa.
27. Ndipo kukadakhala kuti mtengo uliwonse umene uli
pa dziko lapansi udasanduka kukhala cholembera ndipo
nyanja kusanduka kukhala inki mothandizidwandi nyanja
zina zisanu ndi ziwiri ndithudi, mawu a Mulungu sakadatha.
Ndithudi Mulungu ndi wamphamvu ndi waluntha.

28. Kalengedwe kanu ndi kuukitsidwa kwanu kwa
akufa si chinthu chovuta ayi. Ndithudi Mulungu ndi
wakumva ndi wowona. 29. Kodi inu simuona mmene
Mulungu amasandulizira usiku kuti ukhale usana ndi
usana kuti ukhale usiku ndipo wapangira dzuwa ndi mwezi
kuti zizikumverani inu? Ndiponso kodi simuona kuti
chilichonse chimayenda m’njira yake mpaka pa nthawi
yokhazikitsidwa ndipo Mulungu amadziwa zonse zimene
inu mumachita? 30. Ichi ndi chifukwa chakuti Mulungu
ndiye choonadi ndipo kuti chimene iwo amapembedza
kuonjezera pa Mulungu ndi chinthu wamba chabe.
Mulungu ndi Wapamwamba ndi Wamkulu.

31. Kodi inu simuona mmene zombo zimayendera pa nyanja
mwachisomo cha Mulungu ndi mmene amakuonetserani
inu zizindikiro zake? Ndithudi muli chiphunzitso mu
zimenezi kwa anthu olimbikira ndiponso kwa oyamika.
32. Ndipo pamene mafunde okhala ngati mapiri awaphimba,
iwo amapempha kwa Mulungu modzichepetsa. Koma Iye
akangowafikitsa bwino pa mtunda, ena a iwo amatsatira
njira ya pakati ndipo palibe amene amakana chiphunzitso

chathu koma yekhayo amene sathokoza ndiponso amene ndi wamwano.

33. Oh anthu inu! Opani Ambuye wanu ndipo liopeni tsiku limene kholo silidzathandiza mwana wake kapena mwana kuthandiza kholo lake. Ndithudi lonjezo la Mulungu ndi loona. Kotero musalole moyo wa padziko lino lapansi kuti ukunyengeni inu kapena kuti Satana akunyengeni pa nkhani zokhudza Mulungu.
34. Ndithudi Mulungu ndiye yekha amene amadziwa za kudza kwake kwa tsiku lachiweruzo. Ndiye amene amatsitsa mvula ndiponso amadziwa zimene zili m'mimba mwa akazi. Ndipo palibe amene amadziwa zimene zingamuonekere mawa ndipo palibe amene amadziwa dziko limene adzafere. Ndithudi Mulungu ndi Wodziwa ndi Wozindikira.

Sura 32 • Sajdah

# Sajda

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni chosatha.

1. *Alif Lam Mim.*

2. Ichi ndi chivumbulutso cha Buku Lopatulika limene mulibe zokayikitsa ndi chochokera kwa Ambuye wa zolengedwa zonse.
3. Kodi kapena iwo amati wapeka yekha? Iyayi, ndi choonadi chochokera kwa Ambuye wake kuti uchenjeze anthu amene kuyambira kale mchenjezi sanadze kwa iwo, kuti iwo akhoza kutsatira njira yoyenera.

4. Mulungu ndiye amene adalenga kumwamba ndi dziko

lapansi ndi zonse zimene zili m'menemo m'masiku asanu
ndi limodzi. Ndipo atatero Iye adabuka pa mpando
wake Wachifumu. Inu mulibe wokuyang'anirani kapena
wokuthandizani kupatula Iye yekha. Kodi simungaganize?
5. Iye amalamulira zinthu kuchokera kumwamba mpaka
pa dziko lapansi ndipo zidzakwera kudza kwa Iye
m'tsiku limene muyeso wake ungathe kuyerekezedwa ndi
zaka chikwi chimodzi mwa chiwerengero chomwe inu
mumachidziwa. 6. Uyu ndiye wodziwa zobisika ndi zooneka,
Mwini mphamvu, ndi Mwini chisoni chosatha. 7. Amene
adalenga chilichonse m'maonekedwe abwino. Ndipo
adalenga munthu kuchokera ku dothi. 8. Ndipo adalenga
ana ake kuchokera ku dontho lamadzi onyozeka. 9. Ndipo
iye adamuumba munthu mwaubwino ndipo adamuuzira
Mzimu wake. Ndipo Iye adakupatsani inu makutu, maso
ndi mitima, inu simuthokoza nthawi zambiri.
10. Iwo adati, "Chiyani! Pamene ife taikidwa m'manda,
kodi tingadzalengedwenso?" Ndithudi iwo adakana
kuti adzakumana ndi Ambuye wawo. 11. Nena "Mngelo
wa imfa, amene adasankhidwa kukuyang'anirani inu,
adzakupangitsani kuti mufe. Kotero inu mudzabwerera
kwa Ambuye wanu." 12. Iwe ukadangodzaona mmene anthu
ochimwa adzagwetsera mitu yawo pamaso pa Ambuye
wawo nati, "Ambuye wathu! Ife taona ndipo tamva. Tsopano
tibwezereni pa dziko lapansi ndipo ife tidzagwira ntchito
zachilungamo chifukwa ife, ndithudi, takhulupirira."
13. Ife tikadafuna, ndithudi, tikadatsogolera mzimu
uliwonse ku njira yoyenera. Koma kuti mawu ochokera kwa
Ine adakwanitsidwa. "Ine ndidzadzadza Gahena ndi majini
pamodzi ndi anthu." 14. Lawani chilango tsopano, chifukwa

inu mudaiwala za tsikuli. Ndipo nafenso takuiwalani.
Kotero inu lawani chilango chosatha chifukwa cha
ntchito zanu zoipa. 15. Ndi okhawo amene amakhulupirira
chiphunzitso chathu amene chiphunzitsocho chimati
chikaphunzitsidwa, amagwa pansi kupembedza ndipo
amayamika ndi kulemekeza Mulungu wawo modzichepetsa.
16. Iwo amasiya makama awo ndi cholinga chopempha
kwa Ambuye wawo mwamantha ndi mwa chikhulupiriro.
Ndipo amapereka zaulere kuchokera ku chuma chimene
tidawapatsa. 17. Tsopano palibe munthu amene amadziwa
madalitso amene ali kuwasungira m'nkhokwe ngati
malipiro a ntchito zawo zabwino.

18. Kodi munthu wokhulupirira angafanane ndi munthu
woswa malamulo ndi woipa? Iyayi, sangafanane. 19. Iwo
amene amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino,
adzalandira minda ngati malo awo okhala chifukwa cha
ntchito zawo zabwino zimene anachita. 20. Ndipo iwo
amene amaswa malamulo, malo awo okhala ndi kumoto
ndipo nthawi zonse zimene iwo adzafuna kuchokako,
adzabwezedwanso komweko. Ndipo kudzanenedwa kwa
iwo kuti, "Lawani ululu wa moto umene munkati ndi
bodza." 21. Ndipo, ndithudi, Ife tidzawalawitsa, chilango
cha m'moyo uno chisanadze, chilango choyamba kuti
mwina akhoza kutembenuka. 22. Kodi wolakwa kwambiri
ndani kuposa munthu amene amati akakumbutsidwa
chiphunzitso cha Ambuye wake, iye amabwerera m'mbuyo?
Ndithudi Ife tidzalanga anthu ochimwa.

23. Ndipo, ndithudi, Ife tidamupatsa Buku Mose ndipo
musakayike za kulandira kwake ndipo tidalipanga ilo
kukhala chotsogolera ana a Israyeli. 24. Ndipo tidasankha

pakati pawo, atsogoleri amene amapereka malangizo
potsatira malamulo athu, pamene iwo anali kupirira ndi
kukhulupirira mu chiphunzitso chathu. 25. Ndithudi
Ambuye wako adzaweruza pakati pawo pa tsiku louka
kwa akufa pa nkhani zimene anali kutsutsana. 26. Kodi
icho sichiwaphunzitsa phunziro kuti kodi ndi mibadwo
ingati imene tidaononga iwo asanadze, m'nyumba zawo
zimene amalowa ndi kutulukamo? Ndithudi mu izo muli
chiphunzitso. Kodi iwo sangamve?
27. Kodi iwo saona kuti Ife timagwetsa mvula panthaka
youma ndi kumeretsa mbewu zimene iwo ndi ziweto zawo
zimadya? Kodi alibe maso oti angaone? 28. Iwo amafunsa
kuti "Kodi chiweruzo chimenechi chidzachitika liti
ngati zimene munenazi ndi zoona?" 29. Nena, "Pa tsiku
lachiweruzo, chikhulupiriro cha iwo amene sakhulupirira
sichidzawathandiza ndiponso sadzapeza mpumulo."
30. Kotero asiye okha ndipo dikira ndithudi nawonso ali
kudikira.

Sira 33 • Al-Ahzâb

# Al Ahzab

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Oh iwe Mtumwi! Opa Mulungu ndipo usamvere zonena za
anthu osakhulupirira ndi a chinyengo. Ndithudi Mulungu
ndi wodziwa ndi waluntha. 2. Koma tsatira zonse zimene
zavumbulutsidwa kwa iwe kuchokera kwa Ambuye wako

ndithudi Mulungu amadziwa zimene umachita. 3· Ndipo
ukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu chifukwa Iye ndi
wokwana kukhala wokusamalira iwe.
4· Mulungu sadalenge mitima iwiri m'chifuwa cha munthu,
ndipo Iye sadalenge akazi anu amene mumawasudzula
chifukwa chakuti amalingana ndi amayi anu, ndipo
sadawalenge ana omwe mkazi wanu adabereka ndi
mwamuna wina kukhala ana anu enieni. Zimenezo ndizo
zongokamba zanu chabe koma Mulungu ali kukuuzani
inu choonadi ndipo Iye amalangiza njira yoyenera.
5· Aitaneni ndi mayina atate awo ana onse omwe mkazi
wanu adaberaka ndi mwamuna wina chifukwa chimenecho
ndicho chilungamo pamaso pa Mulungu. Koma ngati inu
simudziwa mayina atate awo, pamenepo iwo ndi abale anu
m'chipembedzo kapena abwenzi. Koma palibe cholakwa
kwa inu ngati mulakwitsa. Chimene chifunika kwenikweni
ndi cholinga chimene chili mu mtima mwanu. Ndithudi
Mulungu amakhululukira nthawi zonse ndipo ndi mwini
chisoni chosatha.
6· Mtumwi ali ndi udindo waukulu pa anthu okhulupirira
kuposa umene iwo ali nawo pakati pa wina ndi mnzake
ndipo akazi a Mtumwi ali ngati amayi awo. Ndipo ubale wa
magazi amodzi pakati pawo umawabweretsa pafupi wina
ndi mnzake. M'Buku la Mulungu, ubale umene umadza
kwa iwo amene akhulupirira uposa amene amathawa ku
nyumba kwawo. Ngakhale zili choncho inu muyenera
kuonetsa zabwino kwa abwenzi anu. Zimenezi ndizo
zimene zidalembedwa m'Buku la Mulungu.
7· Kumbukira pamene tidalandira lonjezo lochokera kwa
Atumwi ndi kwa iwe. Ndiponso kuchokera kwa Nowa,

Abrahamu, Mose, ndi Yesu mwana wamwamuna wa Maria.
Tidalandira lonjezo lokhazikika kuchokera kwa iwo. 8. Kuti
Mulungu akhoza kufunsa anthu olungama za chilungamo
chawo ndipo Iye wawakonzera anthu osakhulupirira
chilango chowawa kwambiri.

9. Oh inu anthu okhulupirira! Kumbukirani chisomo cha
Mulungu pa inu pamene kudadza gulu la adani. Koma Ife
tidatumiza, kuti iwagonjetse, mphepo ya mkuntho ndi
Asirikali amene inu simudawaone. Koma Mulungu amaona
zonse zimene mumachita. 10. Pamene iwo adadza kwa inu
kuchokera kumwamba ndi kuchokera padziko lapansi
ndiponso pamene maso adatembenuka, mitima yanu
idafumuka mpaka pakhosi ndipo inu mudayamba kuganiza
maganizo oipa okhudza Mulungu. 11. Pamenepo anthu onse
okhulupirira adayesedwa ndipo adavutitsidwa.

12. Ndipo taona! Anthu onse a chinyengo ndi iwo amene
mu mitima mwawo muli matenda adati, “Mulungu pamodzi
ndi Mtumwi wake sadatilonjeze china chilichonse koma
chinyengo.” 13. Taona! Gulu lina limene lidali pakati pawo
lidati, “Inu anthu a ku Yasrib simungawagonjetse awa
ayi kotero bwererani m’mbuyo!” Ndipo kagulu kena
kamapempha chilolezo kwa Mtumwi ndipo kadati,
“Ndithudi nyumba zathu zilibe woziteteza.” Koma sizinali
choncho ayi koma kuti iwo amangofuna kupeza njira
yothawira. 14. Ndipo mdani akadalowa kudzera pachipata
cha mbali ina ya mzindawu, ndipo iwo akadafunsidwa kuti
aleke chisilamu. Ndithudi, iwo akadachita chomwecho.
Ndipo sakadakayika kutero, ngakhale mpang’ono
pomwe. 15. Komatu iwo adalonjeza kale kwa Mulungu kuti
sadzabwerera m’mbuyo ndipo lonjezo la Mulungu liyenera

kukwaniritsidwa. 16. Nena, “Kuthawa sikudzakuthandizani
inu ngati inu muli kuthawa imfa, kapena kuphedwa.
Ndipo ngakhale kuti inu mungathawe, mudzangosangalala
m’moyo wa pa dziko lino lapansi pa kanthawi kochepa
chabe.” 17. Nena, “Kodi ndani amene angakutetezeni inu
kwa Mulungu ngati iye atafuna kuti akulangeni inu? Kodi
ndani amene akhoza kumuletsa Mulungu ngati atafuna
kuti akuonetseni chifundo chake?” Ndipo iwo sadzapeza
wina kupatula Mulungu kukhala mtetezi kapena mthandizi
wawo.
18. Ndithudi Mulungu amawadziwa onse amene amaletsa
anzawo ndi iwo amene amauza abale awo kuti, “Bwerani
kwa ife.” Pamene iwo sadza ku nkhondo kupatula ochepa.
19. Ndi njiru imene ali nayo pa iwe, pamene choopsa
chidza, iwe udzawaona ali kukuyang’ana, maso awo ali
kutembenuzika, monga munthu amene ali pafupi kufa.
Koma ngati choopsa chidutsa iwo amakunyoza ndi malirime
awo akuthwa chifukwa cha njiru pa zinthu zabwino zimene
uli nazo. Awa sadakhulupirire ndipo Mulungu wasandutsa
zochita zawo kukhala zopanda pake ndipo zimenezi si
zovuta kwa Mulungu. 20. Iwo akuganiza kuti owathandiza
awo alipo ndipo ngati iwo akadabweranso iwo akadafuna
akadakhala ali m’chipululu pamodzi ndi anthu okhala
m’chipululu ndi kufunsa nkhani zokhudza iwe kuchokera
kutali. Ndipo iwo akadakhala pakati panu, akadamenya
nkhondo pang’ono.
21. Ndithudi muli chitsanzo chabwino mwa Mtumwi wa
Mulungu kwa iye amene amakhulupirira mwa Mulungu ndi
tsiku lomaliza ndipo amakumbukira Mulungu kwambiri.
22. Pamene anthu okhulupirira adaona anzawo owathandiza,

iwo adati, “Ichi ndi chimene Mulungu ndi Mtumwi wake
adatilonjeza. Ndithudi Mulungu ndi Mtumwi wake
adatiuza zoona.” Ndipo izi zidaonjezera chikhulupiriro
chawo ndi kudzipereka kwawo kwathunthu. 23. Pakati
pa okhulupirira pali anthu amene amakwaniritsa lonjezo
limene adachita ndi Mulungu. Ena mwa iwo adafa ndipo
ena akadadikira. Koma iwo sadasinthe maganizo ngakhale
pang’ono. 24. Kuti Mulungu akhoza kupereka malipiro
kwa anthu olungama chifukwa cha chilungamo chawo
ndi kulanga anthu a chinyengo ngati chimenecho ndicho
chifuniro chake kapena kuwakhululukira chifukwa
Mulungu ndi wokhululukira ndi Mwini chisoni chosatha.

25. Ndipo Mulungu adawabweza anthu osakhulupirira
atakwiya. Iwo sadapeze chabwino china chilichonse ndipo
Mulungu adawathandiza anthu okhulupirira pomenya
nkhondo. Ndipo Mulungu ndi wamphamvu zambiri.
26. Ndipo anthu a m’Buku amene adawathandiza iwo,
Mulungu adawachotsa kumalo awo okhazikika ndipo
adakhazika mantha m’mitima mwawo, kotero inu
mudapha ena ndi ena mudawagwira ukapolo. 27. Ndipo
Iye adakupatsani dziko lawo, nyumba zawo, ndi katundu
wawo ndi dziko limene inu simuyendamo. Mulungu ali ndi
mphamvu pa chinthu china chilichonse.

28. Oh iwe Mtumwi! Auze akazi ako kuti, “Ngati inu
mukonda moyo wa dziko lino ndiponso zosangalatsa zake,
bwerani, ine ndidzakupatsani zosangalatsa zake ndipo
ndidzakulolani kuti muchoke bwinobwino.” 29. Ndipo ngati
inu mufuna Mulungu ndi Mtumwi wake ndi moyo umene
uli nkudza, ndithudi, Mulungu wawakonzera mphotho
yaikulu anthu ochita zabwino amene ali pakati panu. 30. Oh

inu akazi a Mtumwi! Aliyense wa inu amene achita choipa
poyera, chilango chake chidzaonjezedwa kawiri ndipo
kutero ndi kwapafupi kwa Mulungu.
31. Ndipo aliyense wa inu amene ndi omvera Mulungu
ndi Mtumwi wake ndipo amachita ntchito zabwino, Ife
tidzamupatsa malipiro ake kawiri ndipo tamukonzera
iye chakudya cholemekezeka. 32. Oh inu akazi a Mtumwi!
Inu simuli akazi wamba. Ngati inu mumaopa Mulungu,
muziwayankhula mawu okoma chifukwa mwina anthu
amene mu mtima mwawo muli matenda akhoza kuyamba
kukusirirani. Koma yankhulani mawu abwino.
33. Ndipo khalani mwakachetechete m’nyumba zanu
ndipo musachite zinthu zoipa zoti muonekere poyera
monga mmene amachitira anthu nthawi yaumbuli. Ndipo
pitirizani kupemphera, perekani msonkho wothandiza
anthu osauka ndipo muzimvera Mulungu ndi Mtumwi
wake yemwe. Ndipo Mulungu angofuna kuchotsa uve
umene uli mwa inu anthu a pabanja lake, ndikukuyeretsani
inu. 34. Ndipo kumbukirani chimene chaphunzitsidwa
kwa inu m’nyumba mwanu cha zizindikiro za Mulungu
ndi luntha lake. Chifukwa Mulungu ndiye mwini chifundo
ndipo amadziwa chilichonse.
35. Ndithudi a Chisilamu amene amakhulupirira
ndi amuna ndi akazi okhulupirira, amuna ndi akazi a
chilungamo, amuna ndi akazi opirira, amuna ndi akazi
ofatsa, amuna ndi akazi othandiza osauka, amuna ndi akazi
osala, ndi amuna ndi akazi osachita chiwerewere ndi amuna
ndi akazi amene amakumbukira Mulungu kwambiri; kwa
anthu onse otere, Mulungu wawakonzera chikhululukiro
ndi mphotho yaikulu. 36. Si koyenera kwa munthu

wokhulupirira wamwamuna kapena wamkazi kuti pamene
nkhani yalamulidwa ndi Mulungu ndi Mtumwi wake, kuti
anene china chilichonse pa chiweruzo cha nkhaniyo. Ngati
wina samvera Mulungu ndi Mtumwi wake, ndithudi, iye ali
wosochera moonekeratu.

37. Ndi pamene iwe udamuuza wina amene adalandira
chisomo cha Mulungu ndi chifundo chake kuti, "Musunge
mkazi wako ndipo uope Mulungu." Ndipo iwe udabisa
mu mtima mwako zimene Mulungu akadaulula ndipo iwe
udaopa anthu pamene kunali koyenera kuti uziopa Mulungu.
Ndipo pamene Zaid adamusudzula iye, tidamukwatitsa
iye kwa iwe ndi cholinga chakuti kutsogolo kusadzakhale
vuto kwa anthu okhulupirira pa nkhani ya ukwati
wokhudzana ndi ana owapeza pamene iwo asudzulana.
Ulamuliro wa Mulungu uyenera kukwaniritsidwa.
38. Palibe vuto kwa Mtumwi pa zimene Mulungu wamupatsa
ngati udindo wake. Chidali chizolowezi cha Mulungu kwa
anthu amene adalipo kale. Ndipo ulamuliro wa Mulungu
ndi wokhazikika. 39. Iwo amene amalalikira uthenga wa
Mulungu ndipo amene amamuopa Iye, iwo saopa wina
aliyense koma Mulungu ndipo Mulungu ndi wokwanira
kubwezera. 40. Muhammad si atate wa wina aliyense wa
inu koma iye ndi Mthenga wa Mulungu ndi womaliza wa
Atumwi a Mulungu. Ndipo Mulungu amadziwa chinthu
china chilichonse.

41. Oh inu anthu okhulupirira! Kumbukirani Mulungu
ndipo muzimukumbukira pafupipafupi. 42. Ndipo
muyamikeni m'mawa ndi madzulo aliwonse. 43. Ndiye
amene amapereka madalitso ake pa inu ndipo angelo ake
amachita chimodzimodzi kuti Iye akhoza kukuchotsani

inu ku mdima kupita kowala. Ndipo Iye ndi wachifundo
kwa okhulupirira. 44. Kulonjerana kwawo pa tsiku limene
adzakumana naye kudzakhala adzati,"Mtendere". Ndipo
Iye wawakonzera mphotho yolemekezeka.
45. Oh iwe Mtumwi! Ndithudi takutumiza iwe ngati
mboni ndi wobweretsa nkhani yabwino ndi wochenjeza.
46. Ngati munthu woitana anthu kuti adze kwa Mulungu
ndi chilolezo chake ndiponso ngati Muuni. 47. Kotero
auze nkhani yabwino anthu okhulupirira kuti adzalandira
mphatso yaikulu kuchokera kwa Mulungu. 48. Ndipo
usamvere zilakolako za anthu osakhulupirira ndi za
anthu a chinyengo. Usalabadire zonena zawo koma
ika chikhulupiriro chako mwa Mulungu. Mulungu ndi
wokwana kukhala Mtetezi.
49. Oh inu anthu okhulupirira! Pamene mukwatira akazi
okhulupirira ndipo muwasudzula musanalowane nawo,
palibe nthawi yoyembekezera pakhomo panu. Kotero
asanachoke apatseni mphatso yawo ndipo alekeni kuti
achoke mwaubwino.
50. Oh iwe Mtumwi! Takulola kukhala ndi akazi onse
amene iwe wapereka chiongo chawo ndi iwo amene
ndi akapolo ako kuchokera kugulu limene lidagwidwa
pankhondo ndipo Mulungu wakupatsa iwe; ana a akazi a
atsibweni ndi azakhali ako, a kuchimuna kapena kuchikazi
amene adachoka pamodzi ndi iwe. Ndiponso mkazi wina
aliyense wokhulupirira amene adzipereka yekha kwa
Mtumwi ngati Mtumwi afuna kumukwatira iye. Chilolezo
ichi ndi cha iwe wekha osati cha anthu onse okhulupirira.
Ife tikudziwa chimene tawasankhira iwo zokhudza akazi
awo ndi akapolo amene iwo amasunga, ndi cholinga

chakuti pasadzakhale vuto kwa iwe. Ndipo Mulungu
amakhululukira nthawi zonse ndipo ndiye Mwini chisoni
chosatha.
51. Iwe ukhoza kumusiya aliyense wa iwo amene wafuna
ndipo ukhoza kutenga aliyense wa iwo amene wafuna ndi
aliyense wa iwo amene udawasiya pa kanthawi kochepa.
Palibe cholakwa kwa iwe pochita izi kuti maso awo azizire
ndiponso onse asadandaule ndi zimene uwapatsa. Ndipo
Mulungu amadziwa zinthu zonse zomwe zili m'mitima
mwanu. Mulungu amadziwa zonse ndiponso ndi wopirira.
52. Iwe siuloledwa kukwatiranso akazi ena pambuyo pa awa
kapena kuwasintha kuti upeze akazi ena ngakhale kuti
kukongola kwawo kuli kukusangalatsa kupatula akapolo
amene uli nawo. Ndipo Mulungu amayang'anitsitsa pa
zinthu zonse.
53. Oh inu anthu okhulupirira! Musamalowe m'nyumba za
Mtumwi pokhapokha chilolezo chitaperekedwa kwa inu
kuti mukadye chakudya osati kukadikira chakudya mpaka
pamene chiphikidwa. Koma pamene mwaitanidwa lowani
ndipo pamene mumaliza kudya chokani. Musayembekeze
kumvetsera nkhani. Ndithudi zimenezi zimamupatsa
Mtumwi mavuto koma iye amachita nanu manyazi pamene
Mulungu sachita manyazi kuulula choonadi. Ndipo ngati
inu mufunsa katundu wina aliyense, funsani kuchokera
ku malo osaonekera. Ichi ndi chabwino kwa inu ndiponso
kwa iwo ndipo si koyenera kuti inu mumupatse mavuto
Mtumwi wa Mulungu kapena kuti inu mukwatire akazi ake
iye atawasiya. Ndithudi chimenechi ndi chinthu choipa
pamaso pa Mulungu. 54. Ngati inu muchita chinthu poyera

kapena mobisa, ndithudi, dziwani kuti Mulungu amadziwa
zinthu zonse.
55. Palibe cholakwa kwa iwo pa nkhani zokhudza atate
awo kapena ana awo kapena abale awo kapena ana a abale
awo kapena akazi awo kapena atumiki awo. Ndipo opani
Mulungu. Ndithudi, Mulungu ndi mboni pa chinthu china
chilichonse.
56. Ndithudi Mulungu ndi angelo amamudalitsa Mtumwi
wake. Oh inu anthu okhulupirira! Pemphani madalitso
kuti adze pa iye ndipo mulonjereni ndi malonje abwino.
57. Ndithudi iwo amene amanena zinthu zoipa zokhudza
Mulungu ndi Mtumwi wake, Mulungu anawatemberera
iwo m'moyo uno ndiponso adzawatemberera m'moyo
umene uli nkudza ndipo wawakonzera chilango chochititsa
manyazi. 58. Ndipo iwo amene amayankhula zinthu zoipa
zokhudza anthu a amuna okhulupirira ndi anthu a akazi
okhulupirira, pamene iwo sadalakwe, iwowo ali pamlandu
wonamizira ndi wochita tchimo looneka.
59. Oh iwe Mtumwi! Auze akazi ako ndi ana ako, akazi
ndi akazi a anthu okhulupirira kuti azivala moyenera
zovala zawo zapamwamba zoonjezera pa zovala zomwe
avala mkati. Zimenezi zidzakhala zabwino kuti akhoza
kudziwika nazo ndipo kotero iwo sadzavutitsidwa ayi.
Ndipo Mulungu ndi wokhululukira ndi Mwini chisoni
chosatha. 60. Ngati anthu achinyengo pamodzi ndi iwo
amene m'mitima mwawo muli matenda ndiponso anthu
amene amayambitsa chisokonezo mu mzinda, saleka
mchitidwe oterewu,** ndithudi, Ife tidzalimbana nawo
ndipo iwo sadzakhala pafupi ndi inu kupatula nthawi
yochepa. 61. Iwo ndi otembereredwa. Paliponse pamene

adzapezeka iwo adzagwidwa ndi kuphedwa mwankhanza. 62. Amenewa ndiwo adali machitidwe a Mulungu kwa anthu akale ndipo inu simudzapeza chosintha m'machitidwe a Mulungu.

63. Anthu amakufunsani za ola. Nena kuti, "Mulungu yekha ndiye amene amadziwa za ilo. Kodi chidzakudziwitsani ndi chiyani za olali? Mwinatu lili pafupi!" 64. Ndithudi Mulungu watemberera anthu osakhulupirira ndipo wawakonzera moto woyaka. 65. Adzakhalamo mpaka kalekale ndipo iwo sadzapeza mtetezi kapena wowathandiza. 66. Pa tsiku limene nkhope zawo zidzalangizidwe moto, iwo adzati, "Kukadakhala bwino kuti tikadamvera Mulungu ndi kumvera Mtumwi" 67. Ndipo iwo adzati, "Oh Ambuye wathu! Ndithudi ife tidamvera atsogoleri athu ndi akuluakulu athu kotero iwo adatisocheretsa." 68. "Oh Ambuye wathu! Apatseni iwo chilango chowirikiza ndipo atembereireni iwo ndi matemberero ochuluka."

69. Oh inu anthu okhulupirira! Musakhale ngati anthu amene adayankhula zinthu zoipa zokhudza Mose. Koma Mulungu adatsutsa zonse zimene anali kunena za Mose. Ndipo iye anali wolemekezeka kwa Mulungu. 70. Oh inu anthu okhulupirira! Opani Mulungu ndipo muzinena mawu abwino. 71. Iye adzasunga ntchito zanu pamalo abwino ndi kukukhululukirani machimo anu. Ndipo aliyense amene amamvera Mulungu ndi Mtumwi wake, ndithudi, iyeyo wapeza chinthu chopambana.

72. Ndithudi Ife tidapereka udindo ndi chikhulupiriro kumwamba, pa dziko ndi pa mapiri koma zonse zidakana kulandira ndipo adauopa. Koma munthu adauvomera. Ndithudi iye ndi wosalungama ndiponso mbuli.

73. Motero Mulungu adzalanga amuna ndi akazi a chinyengo.
Ndiponso amuna ndi akazi opembedza mafano. Ndipo
Mulungu adzakhululukira anthu onse okhulupirira,
amuna ndi akazi. Mulungu ndi wokhululukira ndiponso
mwini chisoni chosatha.

Sura 34 • Saba

## Al Saba

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni chosatha.

1. Kuyamikidwa konse ndi kwa Mulungu Mwini wa
chilichonse chakumwamba ndi dziko lapansi ndipo
kuyamikidwa konse ndi kwake m'dziko limene lili
nkudza. Ndipo Iye ndi waluntha ndi wozindikira. 2. Iye
amadziwa chilichonse chimene chimalowa m'nthaka ndi
chilichonse chimene chimatuluka mu iyo ndi chilichonse
chimene chimatsika kuchokera kumwamba ndi chimene
chimakwera kunka kumwamba. Ndipo Iye ndiye Mwini
chifundo ndi Mwini kukhululukira.

3. Ndipo iwo amene sakhulupirira amati, "Ola silidzabwera
kwa ife." Nena, "Inde! Pali Ambuye wanga, amene amadziwa
zinthu zosaoneka. Ndithudi, olalo lidzadza kwa inu."
Palibe chinthu cholemera ngati mbewu ya mpiru chimene
chimabisika kwa Iye kumwamba kapena pa dziko lapansi
kapena chochepera kuposa ichi kapena chachikulu kuposa
ichi chifukwa zonse ndi zolembedwa bwino m'Buku.
4. Koterokuti Iye akhoza kulipira onse amene amakhulupirira

ndipo amachita ntchito zabwino. Awa ndiwo amene
adzakhululukidwa ndiponso adzalandira malipiro abwino.
5. Ndipo iwo amene amalimbikira kutsutsa chivumbulutso
chathu, awa ndiwo amene chilango chowawa ndi chonyansa
chili kuwadikirira. 6. Ndipo iwo amene adapatsidwa nzeru
amaona kuti chimene chapatsidwa kwa iwe kuchoka kwa
Ambuye wako ndi choonadi ndipo chimatsogolera ku njira
ya Mwini mphamvu ndi Mwini kuyamikidwa.
7. Ndipo iwo amene sakhulupirira amati, "Kodi
tingakulangizeni amene amakuuzani kuti pamene inu
musanduka dothi mudzalengendwanso kukhala m'badwo
watsopano?" 8. Kodi iye wapeka bodza lokhudza Mulungu
kapena iye ndi wamisala? Iyayi! Iwo ndi amene sakhulupirira
m'moyo umene uli nkudza ndipo ali mu chilango chachikulu
m'maganizo ndiponso ndi olakwa kwambiri. 9. Kodi iwo
saganiza za chimene chili patsogolo pawo ndi chimene
chili pambuyo pawo chokhudza zinthu za kumwamba
ndi pa dziko lapansi? Ngati Ife titafuna, tidzawachotsa pa
dziko kapena kuwabweretsera gulu lochokera kumwamba.
Ndithudi muli chiphunzitso mu chimenechi kwa kapolo
aliyense amene amatembenukira kwa Mulungu.
10. Ndithudi tidamupatsa Davide zabwino zochokera kwa
Ife. Oh inu mapiri! Imbani nyimbo zotamanda pamodzi ndi
iye ndipo pamodzi ndi mbalame. Ndipo tidapanga chitsulo
kukhala chofewa kwa iye. 11. Tidati, "Panga majasi okwanira
ndipo khazikitsa nthawi yopangira zovala ndipo chita
ntchito zabwino. Ndithudi Ine ndili kuona chilichonse
chimene umachita."
12. Ndipo tidalenga mphepo kukhala yoleza kwa Solomoni
imene inali kuyenda ulendo wa mwezi umodzi masana ndi

ulendo wa mwezi umodzi usiku. Ndipo tidalenga kasupe
amene anali kumutulutsira mkuwa. Ndipo padali majini
amene anali kumugwirira ntchito ndi chilolezo cha Ambuye
wake ndipo aliyense amene sanali kumvera malamulo athu,
tinali kumulanga ndi moto. 13. Iwo adamuchitira zonse
zimene ankazifuna, malinga ndi zithunzithunzi ndi mbiya
zazikulu zothirira maluwa ndi zophikiramo zokhazikika.
Thokozani a m'banja la Davide! Koma ochepa mwa akapolo
anga ndiwo amathokoza.

14. Ndipo pamene tidalamula kuti afe, palibe china
chilichonse chimene chidawadziwitsa kuti wafa koma
mphutsi imene inali kudya ndodo yake ndipo pamene iye
adagwa, majini adadziwa kuti iwo akadadziwa za zinthu
zobisika, sakadapitirira kugwira ntchito yowawa yodikira.

15. Ndithudi kunali chizindikiro kwa onse a Saba
m'chikhalidwe chawo. Minda iwiri ku dzanja lamanja ndi
minda iwiri kudzanja lamanzere. Idyani zabwino zochokera
kwa Ambuye wanu ndipo mumuyamike Iye. Kwa iye kuli
dziko labwino ndiponso ndi Ambuye wokhululukira.
16. Koma iwo sadamvere ayi. Kotero ife tidawatumizira
madzi osefukira kuchokera ku madamu amene sadathe
kuwatseka ndipo m'malo mwa minda yawo iwiri, Ife
tidawapatsa minda iwiri yobereka zipatso zowawa ndi
mitengo ina ya minga. 17. Ife tidawalanga chifukwa cha
kusakhulupirira kwawo ndipo Ife sitilanga wina aliyense
koma anthu osathokoza.

18. Ndipo tidakhazikitsa pakati pawo mizinda imene
tidaidalitsa ndi mizinda ina imene imaoneka msanga ndipo
tidawakonzera ulendo wosavuta. Yendani mwamtendere
usiku ndi usana. 19. Ndipo iwo adati, "Oh Ambuye wathu!

Titalikitsireni mitunda yoti tiziyendamo.” Ndipo iwo
adzipondereza okha. Kotero Ife tidawasandutsa kukhala
nkhani imene imakambidwakambidwa ndipo tidawamwaza
m’magulumagulu. Ndithudi mu chimenechi muli phunziro
kwa aliyense amene amapirira ndi kuthokoza.
20. Ndithudi Satana adakwanitsa zofuna zake pa iwo ndipo
iwo adamutsatira iye kupatula gulu limene lidakhulupirira.
21. Koma iye adalibe ulamuliro pa iwo kupatula kuti
Ife tikhoza kuyesa munthu amene amakhulupirira za
moyo umene uli nkudza ndi iye amene sakhulupirira za
moyowo. Ndipo Ambuye wako amayang’ana chinthu china
chilichonse.
22. Nena, “Itanani onse amene mumawapembedza
kuonjezera pa Mulungu. Iwo alibe ulamuliro pa chinthu
ngakhale chaching’ono cha kumwamba kapena padziko
lapansi ndipo iwo alibe gawo lililonse mu izo. Ndipo iye
alibe wina aliyense womuthandiza kuchokera pakati pawo.
23. Palibe dandaulo limene lingamveke kwa Iye kupatula
lokhalo lochokera kwa iye amene walandira chilolezo
chake. Mpaka pamene mantha adzachotsedwa m’mitima
mwawo, iwo adzati, “Kodi ndi chiyani chimene Ambuye
wanu walamulira?” Iwo adzati, “Choonadi. Ndipo Iye ndi
wapamwamba ndi wamkulu.”
24. Nena, “Kodi ndani amene amakupatsani zabwino
kuchokera kumwamba ndi pa dziko lapansi?” Nena:
“Mulungu.” Ndithudi mwina ife kapena inu muli pa
njira yachilungamo kapena ochimwa zedi. 25. Nena
“Inu simudzafunsidwa za machimo athu ndiponso ife
sitidzafunsidwa za zimene mudachita.” 26. Nena, “Ambuye
wathu adzatisonkhanitsa tonse pamodzi ndipo pomaliza

adzaweruza pa mikangano yathu mwa choonadi ndi
mwachilungamo. Iye ndiye amene adzaweruza. Ndipo Iye
amadziwa zinthu zonse.” 27. Nena, “Ndilangizeni zimene
inu muli kuzipembedza kuonjezera pa Mulungu. Iyayi! Iye
ndi Mulungu, Mwini mphamvu ndi Mwini nzeru.”
28. Takutumiza iwe kwa anthu a mitundu yonse kuti
uwauze uthenga wabwino ndi kuwachenjeza. Koma anthu
ambiri sadziwa zimenezi. 29. Iwo amati, “Kodi lonjezo ili
lidzakwaniritsidwa liti ngati uli kunena zoonadi?” 30. Nena,
“Tsiku lanu lidakhazikika kale ndipo inu simungaonjezere
kapena kubwezera m’mbuyo ngakhale ola limodzi.”
31. Ndipo iwo amene sakhulupirira amati, “Ife
sitidzakhulupirira mu Buku la Korani kapena mu icho
chimene chidadza kale. Ndipo iwe ukadaona pamene
anthu ochita zoipa adzaimirira pamaso pa Ambuye wawo
ali kudzudzulana wina ndi mnzake! Iwo amene ankati ndi
ofoka adzanena kwa anthu opulupudza kuti, “Pakadapanda
inu, ndithudi, ife tikadakhala okhulupirira!” 32. Iwo amene
adali onyada adzati kwa iwo amene ankati ndi ofoka kuti,
“Kodi ife tinakukanizani kutsatira langizo pamene lidadza
kwa inu? Iyayi. Nokha mudachimwa.” 33. Iwo amene ankati
ndi ofoka adzati kwa iwo amene adali onyada, “Iyayi! Inu
munkakonza chiwembu usiku ndi usana ndipo mumatiuza
ife kuti tisakhulupirire mwa Mulungu koma kukhazikitsa
mafano kuonjezera pa Iye.” Ndipo iwo adzabisa
kukhumudwa kwawo pamene adzaone chilango ndipo Ife
tidzaika magoli m’makosi mwa iwo amene sadakhulupirire.
Iwo sadzakhululukidwa pa zimene adachita.
34. Ife sitidatumizepo Mchenjezi ku mzinda wina uliwonse
umene anthu ake opeza bwino sadanenepo mawu oti,

"Ndithudi ife sitikhulupirira uthenga umene watumizidwa."
35. Ndipo iwo adati, "Ife tili ndi chuma chambiri ndiponso
ana, kotero ife sitidzalangidwa ayi." 36. Nena, "Ndithudi
Ambuye wanga amapereka moolowa manja kwa aliyense
amene Iye wamufuna ndi monyalapsa kwa aliyense amene
Iye wamufuna. Koma anthu ambiri sadziwa." 37. Si chuma
kapena ana anu amene adzakufikitsani kufupi ndi Ife
koma okhawo amene amakhulupirira ndi kuchita ntchito
zabwino. Otere ndiwo amene ali ndi malipiro odzala
manja awiri chifukwa cha ntchito zawo ndipo adzakhala
mwamtendere pamalo olemekezeka. 38. Ndipo onse amene
amalimbikira kutsutsa chiphunzitso chathu adzalangidwa.
39. Nena, "Ndithudi Ambuye wanga amapereka moolowa
manja kwa aliyense wa akapolo ake amene wamufuna
ndipo amachepetsa za aliyense amene wamufuna. Ndipo
chilichonse chimene mupereka, Iye amalipira mowirikiza
ndipo Iye ndiye amapereka kwambiri."

40. Patsiku limene adzawasonkhanitsa onse pamodzi ndi
kuwafunsa Angelo kuti, "Kodi ndinu amene anthu awa anali
kupembedza?" 41. Angelo adzati, "Ulemerero ukhale kwa
Inu! Inu ndinu Mtetezi wathu osati iwo ayi. Iyayi! Iwo anali
kupembedza majini ndipo ambiri a iwo anali kukhulupirira
mwa iwo." 42. Kotero patsiku limeneli, iwo sadzakhala ndi
mphamvu zothandizana kapena kupwetekana wina ndi
mnzake. Ndipo Ife tidzati kwa anthu ochimwa. "Lawani
chilango cha moto chimene inu munali kuchikana."

43. Pamene chiphunzitso chathu chomveka
chimalalikiridwa kwa iwo, iwo amati, "Uyu ndi munthu
amene afuna kukuletsani chipembedzo cha makolo anu."
Ndipo iwo amati, "Ili ndi bodza limene wapeka." Ndipo

anthu osakhulupirira, pamene choonadi chidza kwa iwo
amati, "Awa ndi matsenga." 44. Ife sitidawatumizire mabuku
kuti awaphunzitse kapena kuwatumizira Atumwi iwe
usanadze ngati wowachenjeza. 45. Ndipo iwo amene analipo
kale iwo asanadze adakana choonadi. Awa sadalandire,
ngakhale gawo la chikhumi la zimene tidawapatsa iwo.
Komabe pamene iwo adakana Atumwi anga, kodi chilango
changa chinali chowawa bwanji?
46. Nena, "Ine ndili kukufunsani kuti muchite chinthu
chimodzi choti muime pamaso pa Mulungu awiriawiri
kapena aliyense payekha ndipo muganize painu nokha.
M'bale wanu si wamisala ayi. Iye ali kungokuchenjezani
chilango chowawa chisanadze." 47. Nena, "Malipiro ena
aliwonse amene ndidakufunsani ndi anu chifukwa malipiro
anga ali ndi Mulungu ndipo Iye ndi mboni pa zinthu zonse."
48. Nena, "Ndithudi Ambuye wanga amanena zoona ndipo
ndi Mwini wodziwa zinthu zobisika." 49. Nena, "Choonadi
chadza ndipo bodza latha ndipo silidzabwereranso."
50. Nena, "Ngati ine ndilakwa, ndilakwira mzimu wanga
ndipo ngati ndatsatira njira yolungama ndi chifukwa cha
zimene Ambuye wanga amavumbulutsa kwa ine. Ndithudi
Iye amamva ndipo ali pafupi."
51. Ndipo iwe ukadangoona nthawi imene adzachite
mantha komabe iwo sadzathawa ndipo iwo adzagwidwa
asanapite patali. 52. Ndipo iwo adzati, "Ife tili kukhulupirira."
Kodi kukhulupirira kwawo kudzawathandiza bwanji
kuchokera kutali? 53. Ndipo iwo sadakhulupirire kale ndipo
amanena kuti ndi nkhani za m'maluwa kuchokera kutali.
54. Ndipo chipupa chidzakhazikitsidwa pakati pawo ndi

zofuna zawo monga momwe adachitira ndi anthu ena a kale. Ndithudi iwo ndi okayika kwambiri.

SURA 35 • AL-FÂTIR

# AL FATIR

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni chosatha.

1. Kuyamikidwa konse ndi kwa Mulungu, Namalenga wakumwamba ndi dziko lapansi, amene adalenga angelo, atumwi ouluka, amapiko awiri, atatu ndi anayi. Iye amachulukitsa zolengedwa mwachifuniro chake. Ndithudi Mulungu ali ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse.
2. Chimene Mulungu, mwachifundo chake, amapereka kwa anthu palibe amene angawalande, ndipo chilichonse chimene Iye awamana palibe wina amene angawapatse. Iye ndiye Mwini mphamvu ndiponso Mwini nzeru.
3. Oh anthu inu! Kumbukirani zokoma zimene Mulungu adakupatsani! Kodi pali Namalenga wina kupatula Mulungu amene akhoza kukupatsani zokoma kuchokera kumwamba kapena padziko lapansi? Kulibe mulungu wina koma Iye yekha. Nanga ndi chifukwa chiyani mumanyengedwa?
4. Ndipo ngati akuti iwe ndi wabodza, ndithudi, Atumwi amene adadza iwe usanabadwe nawonso adatchulidwa kuti ndi abodza ndipo ndi kwa Mulungu kokha kumene zinthu zonse zidzabwerera.
5. Anthu inu! Ndithudi lonjezo la Mulungu ndi loona, kotero musalole zokoma za m'moyo uno kuti zikunyengeni

ndiponso musalole mdyerekezi kuti akunyengeni zokhudza Mulungu. 6. Ndithudi Satana ndi mdani wanu, kotero dziwani kuti iye ndi mdani wanu. Iye amangoitana gulu lake kuti akhoza kukakhala nalo ku moto woyaka. 7. Kwa iwo amene sakhulupirira, iwo adzalandira chilango chowawa ndipo iwo amene amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino, iwo adzakhululukidwa ndi kulandira mphotho yaikulu.

8. Kodi iye,amene zoipa zake zimaoneka ngati zabwino, moti akamaziona amati ndi zabwino? Ndithudi Mulungu amasocheretsa aliyense amene amamufuna ndiponso amatsogolera aliyense amene wamufuna. Kotero usavutike mu mtima mwako chifukwa cha iwo. Ndithudi Mulungu amadziwa zonse zimene amachita.

9. Ndipo Mulungu ndiye amene amatumiza mphepo imene imayendetsa mtambo, ndipo timauyendetsa kudziko lakufa ndipo ndi iwo timapereka moyo ku nthaka ikafa. Kumeneko ndiko kuuka kwa akufa. 10. Aliyense amene afuna ulemu ndi mphamvu ndi kwa Mulungu kumene kuli ulemu ndi mphamvu. Kwa Iye ndiko kumene kumapita mawu abwino ndipo ntchito zabwino amazinyamula. Akakhala iwo amene amakonza ntchito zoipa, iwo adzalandira chilango chowawa ndipo chikonzero chawo chidzafafanizidwa. 11. Ndipo Mulungu adakulengani inu kuchokera ku dothi, kenaka adakulengani kuchokera ku dontho la umuna ndipo adakupangani inu awiriawiri ndipo palibe mkazi amene amaima kapena kubala kupatula ndi chilolezo chake. Ndipo palibe aliyense amene moyo wake umapitirizidwa kapena kuchepetsedwa kupatula zimene

zidalembedwa m'Buku Lopatulika. Ndithudi zimenezi ndi
za pafupi ndi Mulungu.
12. Ndipo nyanja ziwiri sizingakhale zofanana kwenikweni.
Ina ndi ya madzi ozuna amene amatha ludzu chifukwa cha
kukoma kwake, okoma kumwa; ndipo ina ndi yamchere,
imene imatentha chifukwa cha mchere. Komabe
kuchokera mu zonse inu mumadya zakudya zabwino ndipo
mumatulutsamo zinthu zosangalatsa zimene mumavala.
Ndipo inu mumaona zombo zilikuyenda m'mafunde kuti
inu muthe kufunafuna zokoma za Mulungu ndiponso
kuti muzithokoza. 13. Iye amasanduliza usiku kuti ukhale
usana ndipo amasanduliza usana kuti ukhale usiku ndipo
Iye adalamula dzuwa ndi mwezi kumvera malamulo ake.
Iye adalamula chilichonse kuti chiziyenda m'njira yake
mpaka pa tsiku lokhazikitsidwa. Iye ndi Mulungu,Ambuye
wanu; wake ndi Ufumu ndipo iwo amene mumapembedza
poonjezera pa Mulungu salamulira chinthu ngakhale
chaching'ono. 14. Ngati inu muwapempha iwo sadzamva
kupempha kwanu ndipo ngati iwo akadamva iwo sangathe
kuyankha mapemphero anu. Ndipo pa tsiku lachiweruzo
iwo adzakukanani inu. Ndipo palibe wina amene
angakuuzeni inu kuposa Iye amene amadziwa chilichonse.
15. Anthu inu! Ndinu amene mumafuna Mulungu
ndipo Mulungu ndiye amene ali woima payekha ndi
woyamikiridwa. 16. Ngati Iye atafuna akhoza kukuchotsani
ndi kubweretsa m'badwo wina watsopano. 17. Ndipo kutero
si kovuta kwa Mulungu. 18. Ndipo mzimu wolemedwa
sungathe kunyamula katundu wa mzimu wina wolemedwa
ndipo ngati mzimu wina wolemedwa utalilira mzimu
wina wolemedwa kuti uunyamulire katundu wake,

winawo siungathe kunyamula katunduyo ngakhale kuti
mizimuyo itakhala pa chibale. Achenjeze okhawo amene
amaopa Ambuye wawo mwamseri ndipo amakwaniritsa
mapemphero, ndipo aliyense amene adziyeretsa, amatero
populumutsa mzimu wake. Ndi kwa Mulungu kokha
kumene onse adzabwerera.
19. Ndipo anthu akhungu ndi openya safanana. 20.
Ngakhalenso usiku ndi usana sizifanana. 21. Ngakhalenso
mthunzi wozizira kwambiri ndi kutentha kwa dzuwa
sizingafanane. 22. Ndipo zamoyo ndi zakufa sizifanana.
Ndithudi Mulungu akhoza kumupanga aliyense amene
wamufuna kuti amve koma iwe siungathe kuwauza iwo
amene ali m'manda kuti amve. 23. Iwe ndiwe wochenjeza
kwambiri. 24. Ndithudi Ife takutumiza iwe ndi choonadi
ngati wotenga nkhani zabwino ndi mchenjezi ndipo palibe
mtundu wa anthu umene sadakhale ndi mchenjezi pakati
pawo kalelo. 25. Ndipo ngati iwo akuti iwe ndiwe wabodza,
nawonso amene adalipo kale, adawatcha Atumwi awo kuti
ndi abodza. Atumwi awo adadza kwa iwo ndi chiphunzitso
chomveka ndi mawu opatulika ndi Buku la muuni.
26. Kotero ndidawalanga anthu onse amene sadakhulupirire.
Kodi chilango changa chidali chotani?
27. Kodi inu simuona mmene Mulungu amagwetsera
mvula kuchokera ku mitambo? Ndi mvulayo Ife
timameretsa mbewu za maonekedwe osiyanasiyana.
Ndipo m'mapiri muli njira zoyera ndi zofiira, zooneka
m'maonekedwe osiyanasiyana ndi zina zakuda. 28. Pali
kusiyana m'maonekedwe pakati pa anthu, zolengedwa ndi
zinyama. Iwo amene amaopa Mulungu pakati pa akapolo

ake ndiwo amene ali ndi nzeru chifukwa Mulungu ndi
wamphamvu zambiri ndi wokhululukira nthawi zonse.
29. Iwo amene amawerenga Buku la Mulungu, amene
amapitiriza kupemphera nthawi zonse ndipo amapereka
chaulere pa katundu amene tawapatsa mwamseri kapena
poyera, ayenera kukhulupirira m'malonda amene sadzatha
ayi. 30. Kuti Iye akhoza kuwalipira mphotho zawo zonse ndi
kuwapatsa zambiri kudzera m'chisomo chake. Ndithudi
Iye ndi wokhululukira amene amachulukitsa malipiro.
31. Ndipo chimene tavumbulutsa kwa iwe kuchokera
m'Buku ndi choonadi chimene chitsimikiza zimene
zidalipo kale. Ndithudi Mulungu amadziwa ndipo amaona
zochita za akapolo ake.
32. Ndipo tidapereka Buku kuti lisungidwe ndi anthu
amene adali pakati pa akapolo athu. Ndipo pakati
pawo pali munthu amene amataya mzimu wake ndipo
pakati pawo pali iye amene amaima pakati ndi pakati
ndiponso pakati pawo pali iye amene amakhala patsogolo
pochita ntchito zabwino ndi chilolezo cha Mulungu.
Umenewu ndiwo ubwino wopambana. 33. Iwo adzalowa
m'minda yokhalitsa ndipo azidzavala zibangiri zagolide
ndi nkhombe ndipo zovala zawo zidzakhala za silika.
34. Ndipo iwo adzati, "Kuyamikidwa konse ndi kwa Mulungu
amene wachotsa chisoni pakati pathu. Ndithudi Ambuye
wathu ndi wokhululukira ndiponso amene amachulukitsa
malipiro." 35. "Amene watikhazika m'nyumba yokhalamo
mpaka kalekale mwachisomo chake. Palibe mavuto amene
adzatipeza kuno ndiponso sitidzakhala otopa."
36. Akakhala iwo amene sakhulupirira, iwo adzakhala
kumoto wa ku Gahena. Iwo siudzawamaliza kuti afe ayi,

ndipo chilango chawo sichidzachepetsedwa. Kotero
ndi mmene timalipirira aliyense wosayamika. 37. Ndipo
iwo adzalira pofuna chipulumutso nati, "Ambuye wathu!
Tichotseni kuno. Ife tikachita zinthu zabwino kusiyana ndi
zimene tinali kuchita". "Kodi Ife sitidakusungeni ndi moyo
nthawi yaitali kuti iye amene amalabadira akadazindikira
za zimenezi? Ndipo kwa inu kudadza mchenjezi kotero
lawani chilango chifukwa munthu wochimwa alibe woti
angamuthandize".
38. Ndithudi Mulungu amadziwa zonse zobisika
zakumwamba ndi pa dziko lapansi. Ndithudi Iye amaona
zimene zili m'mitima mwa anthu. 39. Ndiye amene
adakusankhani kukhala oweruza pa dziko. Kotero
aliyense amene sakhulupirira, kusakhulupirira kwake
kudzamupweteka yekha. Ndipo kusakhulupirira kwawo
sikuonjezera china chilichonse kwa Ambuye wawo
kupatula chidani chokha. Ndipo kusakhulupirira kwawo
sikuonjezera china chilichonse kwa iwo kupatula kutayika.
40. Nena, "Kodi mudayamba mwaganiza za mafano
anu amene mumapembedza kuonjezera pa Mulungu?
Tandilangizani gawo limodzi la dziko limene mafanowo
adalenga? Kodi kapena iwo ali ndi gawo kumwamba?
Kodi kapena Ife tidawapatsa Buku Lopatulika limene iwo
amatsatira chiphunzitso chake? Iyayi! Anthu ochimwa
sakwaniritsa malonjezo pakati pawo koma kunyengana
basi." 41. Ndithudi ndi Mulungu amene amayang'anira
kumwamba ndi dziko lapansi kuti zingaonongeke ndipo
izo zitaonongeka palibe wina amene akhoza kuzikonzanso
kupatula Iye yekha. Ndithudi Iye ndi wopirira ndi
wokhululukira.

42. Ndipo iwo adalumbira motchula Mulungu ndi
molimbika kuti ngati kungadze kwa iwo Mtumwi iwo
adzalandira ulangizi wake kuposa mtundu wina uliwonse.
Koma pamene Mtumwi adadza kwa iwo, kubwera kwake
kudaonjezera kuipa kwawo. 43. Chifukwa cha mwano
ndi chiwembu chimene anali kukonza ndi chifukwa
chakukonza chiwembucho, choipa chidagwa pa onse
amene adakonza chiwembucho. Kodi iwo ayembekeza
kusamalidwa mosiyana ndi anthu akale? Ndipo inu
simudzapeza chosintha m'machitidwe a Mulungu.
44. Kodi iwo sadayende padziko lapansi ndi kuona zimene
zidawachitikira anthu amene adalipo kale pamene
mitundu ya anthuwo idali yamphamvu kuposa iwo? Kulibe
chinthu kumwamba kapena padziko lapansi chimene
chingakhumudwitse Mulungu chifukwa Iye amadziwa
chilichonse ndipo ndi mwini mphamvu zonse.

45. Ndipo Mulungu akamalanga anthu chifukwa cha
zoipa zimene amachita, sipakadakhala cholengedwa
chimene chikadakhala ndi moyo padziko lapansi. Koma
Iye amazisunga mpaka pa nthawi ya malire awo. Ndipo
pamene nthawi yawo ikwana, ndithudi, Mulungu amaona
akapolo ake onse.

# Ya Seen

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni chosatha.

1. *Ya seen*

2. Ndili kulumbira pali Buku la nzeru la Korani. 3. Ndithudi
iwe ndiwe mmodzi mwa amene adatumizidwa. 4. Pa njira
yoyenera. 5. Ichi ndi chivumbulutso cha Mwini mphamvu
ndi Mwini chisoni. 6. Kuti uwachenjeze anthu amene
makolo awo sadachenjezedwe, kotero iwo ndi osamvera.
7. Ndithudi liwu la chilango latsimikizidwa kwa ambiri
a iwo koma iwo sali okhulupirira. 8. Ife taika magoli
m'makosi mwawo, amene afika m'zigama ndipo mitu yawo
yanyamulidwa. 9. Ife taika chotchinga kutsogolo kwawo
ndiponso kumbuyo kwawo ndipo tawakuta maso awo kuti
asaone. 10. Ndi chimodzimodzi kaya uwachenjeza kapena
ayi ndipo iwo sadzakhulupirira. 11. Ukhoza kumuchenjeza
yekhayo amene watsatira chikumbutso ndi kuopa
Mwini Chisoni ngakhale kuti iye sangamuone. Kwa iye
umuuze nkhani yabwino ya chikhululukiro ndi mphotho
yopambana.
12. Ndife amene tidzadzutsa anthu akufa ndi kulemba
ntchito zonse za anthu ndi zizindikiro zimene asiya
m'mbuyo: Talemba zonse mooneka bwino kwambiri
m'buku.
13. Apatse chitsanzo cha anthu a mu mzinda umene
mudadza Atumwi. 14. Pamene Ife tidawatumizira iwo awiri,

iwo adawakana. Motero Ife tidatumizanso wina wachitatu,
ndipo iwo adati, “Ndithudi ife tatumizidwa kwa inu.”
15. Iwo adati, “Inu ndinu anthu ngati ife tomwe. Mwini
chisoni sadavumbulutse china chilichonse! Inu muli
kunama basi.” 16. Iwo adati, “Ambuye wathu akudziwa kuti
ife tatumidwa.” 17. “Udindo wathu ndi wongokuchenjezani
basi.” 18. Anthu adati, “Tili kuona malodza. Ngati mupitiriza
tikuponyani miyala ndipo chilango chowawa chizadza
pa inu.” 19. Iwo adati, “Malodza anu akhale ndi inu! Kodi
chifukwa chakuti mwachenjezedwa? Iyayi koma inu ndinu
anthu ochimwa kwambiri.

20. Nthawi yomweyo munthu wina adadza ali
kuthamanga kuchokera kumbali ina ya mzinda. Iye adati,
“Anthu anga! Tsatirani iwo amene atumidwa ndi Mulungu.”
21. “Atsatireni iwo amene safuna malipiro kuchokera kwa inu
pokukumbutsani mawu a Mulungu ndipo ndi otsogozedwa
bwino.”

22. “Kodi pali chifukwa chotani chimene
chingandilepheretse ine kuti ndim’pembedze Iye
amene adandilenga popeza ndi kwa Iye kumene nonse
mudzabwerera?” 23. “Kodi ine ndizipembedza milungu
ina osati Iyeyo? Ngati ndi chifuniro cha Mwini chisoni
kundizunza, kukhala pakati kwawo sikudzandithandiza
ndipo iwo sadzandipulumutsa ayi.” 24. “Ndithudi
ine ndikadatero, ndikadakhala mu chisokonezo
choonekeratu.” 25. Ndithudi ine ndakhulupirira mwa
Ambuye wanu choncho ndimvereni.” 26. Kudanenedwa
kwa iye kuti, “Lowa mu Paradiso.” Iye adafuula kuti,
“Akadakhala kuti anthu anga adadziwa.” 27. “Mmene

Ambuye wanga wandionetsera chifundo chake kundiika
mugulu la olemekezeka.”
28. Ndipo Ife sitidatumize padziko lapansi, kwa anthu
ake, gulu lochokera kumwamba kuti lilimbane nawo ndipo
sikudali koyenera kuti Ife tichite choncho. 29. Udali mkuwo
umodzi ndipo Oh! Onse adaonongedwa. 30. Kalanga
akapolo anga! Iwo amaseka pofuna kunyoza Mtumwi
aliyense amene adadza kwa iwo. 31. Kodi iwo sadaone
mibadwo yakale imene tidaiononga zaka zikwizikwi
iwo asanabadwe? Ndipo iwo sadzabwereranso. 32. Onse,
popanda opatuka, adzadza kwa Ife.
33. Chizindikiro kwa iwo ndi nthaka yakufa imene
tidaidzutsa ndipo timatulutsa m’nthakamo nthangala
zomwe iwo amadya. 34. Taika m’nthakamo minda ya
mitengo ya tende ndi ya mphesa ndipo timathirira ndi
madzi a m’kasupe. 35. Moti akhoza kumadya zipatso
zake. Si manja awo amene adapanga zimenezi ayi. Kodi
sangathokoze? 36. Ulemerero ukhale kwa Iye amene
adalenga zinthu ziwiriziwiri, (chachimuna ndi chachikazi)
zimene zimamera m’nthaka ndi zina za mtundu wawo ndi
zinanso zimene sazidziwa.
37. Chizindikiro cha kwa iwo ndi usiku. Kuchokera ku
iwo timachotsa usana ndipo iwo amakhala mu mdima.
38. Dzuwa limayenda mofulumira kupita kumalo ake
okapuma. Umenewu ndiwo ulamuliro wa Mwini Mphamvu
zonse ndiponso Wodziwa chilichonse. 39. Ndipo mwezi
tidaulamulira kuti uyende mumsewu wake mpaka pamene
ukamabwerera ngati nthawi yoyamba m’maonekedwe.
40. Dzuwa sililoledwa kupitirira mwezi ndipo usiku siupyola
usana. Chilichonse chimayenda mumsewu wake.

41. Ndipo chizindikiro china kwa iwo ndi chakuti
tidanyamula makolo awo mu chombo chonyamula
katundu. 42. Tidalenga zombo za mtundu umenewu kuti
iwo azikweramo. 43. Timawamiza tikafuna ndipo palibe
amene angawathandize ndipo sangathe kupulumutsidwa.
44. Kupatula kudzera m'chifundo chathu ndi kuwapatsa
chisangalalo cha kanthawi kochepa.

45. Pamene zinenedwa kwa iwo kuti, "Opani chinthu
chimene chili patsogolo panu ndi pambuyo panu kuti
mwina Mulungu angakuonetsereni chifundo" ndipo iwo
samvera ayi. 46. Ndithudi palibe chizindikiro chochokera
kwa Ambuye wawo chimene iwo amachivomera. Ndipo
iwo salabadira. 47. Ndipo pamene auzidwa kuti, "Perekani
gawo la chopereka chaulere pa zinthu zimene Mulungu
wakupatsani." Anthu osakhulupirira amanena kwa anthu
okhulupirira kuti, "Kodi ife tizidyetsa iwo amene Mulungu
atafuna akhoza kuwadyetsa? Ndithudi inu ndi osochera
kwambiri."

48. Iwo amanenanso kuti, "Kodi lonjezo limeneli la
tsiku lachiweruzo lidzatsimikizidwa liti, ngati zimene
uli kunenazi ndi zoona?" 49. Angodikira mkokomo
umodzi wokha basi umene udzadza pa nthawi imene
iwo ali kutsutsana. 50. Iwo sadzakhala ndi mwayi wosiya
mawu kapena kubwerera kwa abale awo. 51. Pamene
lipenga lidzamveka, taona, kuchokera ku manda, anthu
adzathamanga kupita kwa Ambuye wawo. 52. "Tsoka kwa
ife!" Iwo adzatero. "Ndani amene watidzutsa kuchokera
kumalo athu a mpumulo?" Ichi ndi chimene Ambuye
wachifundo adalonjeza. "Atumwi adanenadi zoona!"

53. Ndithudi ndi mfuwu umodzi wokha, onse panthawiyo,
adzasonkhanitsidwa kwa Ife.

54. Patsiku limeneli sipadzakhala mzimu umene
siudzaweruzidwa ndipo inu mudzalandira mphotho
molingana ndi ntchito zanu. 55. Pa tsiku limeneli anthu
okhala ku Paradiso adzakhala osangalala kwambiri.
56. Iwo pamodzi ndi akazi awo, adzakhala m'mithunzi ya
nkhalango, pa mipando yawofowofo. 57. Iwo adzapeza
m'menemo zipatso ndi zina zonse zimene adzafuna.
58. "Mtendere" ndiwo mawu amene adzachokere kwa
Mulungu, Mwini Chisoni.

59. Ndipo Iye adzati, "Khalani kutali inu oipa tsiku
lalero?" 60. "Kodi Ine sindidakuchenjezeni, inu ana a
Adamu, kuti musamagwadire Satana, chifukwa iyeyu ndi
mdani wanu woonekeratu?" 61. "Ndi kuti muzindipembedza
Ine? Ndithudi imeneyo ndiyo njira yoyenera." 62. Koma
iye adasocheretsa anthu ambiri. Kodi mudalibe nzeru?
63. Imeneyi ndiyo Gahena imene munali kulonjezedwa.
64. Lowani m'menemo tsiku lalero ngati chilango, chifukwa
chakusakhulupirira kwanu. 65. Lero, Ife titseka pakamwa
pawo, ndipo manja awo ndi amene ayankhule ndi Ife
ndiponso miyendo yawo ichitira umboni pa ntchito zoipa
zimene anali kuchita.

66. Chikadakhala cholinga chathu, tikadawachititsa
khungu kuti azivutika poyenda. Nanga akadaona bwanji
machimo awo?. 67. Chikadakhala cholinga chathu,
tikadawasintha kuti asanduke china chake pamalo pamene
adaimirira, kuti asapite patsogolo kapena kubwerera
m'mbuyo. 68. Aliyense amene timamukalambitsa,
timam'bwezera ku ubwana. Kodi iwo sangazindikire

chimenechi? 69. Ife sitidamuphunzitse iye ndakatulo ayi ndiponso si koyenera kuti akhale mlakatuli. Ichi si china koma chikumbutso ndi dongosolo la Korani. 70. Limene lichenjeza anthu a moyo ndi kupereka chiweruzo kwa anthu osakhulupirira.

71. Kodi iwo saona kuti pakati pa zinthu zimene tidalenga ndi manja athu tidawalengera nyama zimene iwo amazilamulira? 72. Tidalamula zimenezi kuti zizimvera malamulo awo kuti akhoza kumakwera ndi zina zoti azidya. 73. Ndipo amapezanso phindu lina lolekana. Iwo amamwa mkaka kuchokera ku izo. Kodi iwo sangathokoze? 74. Iwo akhazikitsa milungu ina powonjezera pa Mulungu weniweni, poganiza kuti mwina akhoza kuthandizidwa. 75. Milunguyo siingawathandize. Iwo adzatengedwa mwankhondo kunka ku chilango. 76. Usalole kuti mawu awo akumvetse chisoni. Ife tikudziwa zonse zimene azibisa ndi zonse zimene akuzionetsa.

77. Kodi munthu, sadziwa kuti tidamulenga kuchokera ku dontho la umuna? Koma iye ndi otsutsana ndi Ife poyera. 78. Iye amatifanizira Ife ndi zina zake ndipo amaiwala za chilengedwe chake. Iye amafunsa kuti, “Kodi ndani amene adzapereka moyo ku mafupa oola?” 79. Nena “Iye amene adawalenga poyamba adzawapatsa moyo. Iye amadziwa chilichonse cha zolengedwa zake.” 80. Iye amene amakupatsani moto kuchokera ku mtengo wauwisi umene inu mumawunikira. 81. Kodi Iye amene adalenga kumwamba ndi dziko lapansi, alibe mphamvu zolenga china chake chofanana nazo? Ndithudi ali nazo. Iye ndi Mlengi amene amadziwa chinthu china chilichonse. 82. Ndithudi pamene Iye afuna chinthu amangonena kuti, “Chikhale” ndipo

chimakhaladi. 83. Ulemerero ukhale kwa Iye amene ali ndi
ulamuliro pa chinthu china chilichonse; ndipo ndi kwa Iye
kumene nonse mudzabwerera.

Sura 37 • As-Sâffât

## Al Saffat

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pali iwo amene amasonkhana kukhala pa maudindo
osiyanasiyana. 2. Pali iwo amene amayendetsa mitambo
mwa ubwino. 3. Pali iwo amene amabweretsa m'Buku ndi
Korani kuchokera kwa Mulungu kupita nalo kwa anthu ake.
4. Ndithudi Mulungu wanu ndi mmodzi yekha. 5. Ambuye
wakumwamba ndi dziko lapansi ndi wa zonse zimene zili
m'menemo ndi Ambuye wa dera lililonse lotulukira dzuwa.
6. Ndithudi Ife tidakongoletsa mtambo woyandikira
kwambiri ndi nyenyezi. 7. Ndi kulonda Satana wofukira
8. Kotero iwo sangathe kumvetsera zokambidwa za gulu
lapamwamba chifukwa iwo amapirikitsidwa kuchokera
kumbali iliyonse. 9. Atapirikitsidwa, chawo chidzakhala
chilango chosatha. 10. Kupatula yekhayo amene amakwatula
zinthu mwakuba, ndipo amathamangitsidwa ndi moto
woyaka ndi wowala kwambiri.
11. Ndipo tawafunsa, "Kodi iwo ndi a mphamvu kuposa
zolengedwa zina zimene tidalenga?" Iwo tidawalenga
kuchokera ku dothi lonyata la makande. 12. Iyayi, iwe
udadabwa pamene iwo anali kunyoza. 13. Ndipo iwo

akamaweruzidwa, iwo safuna kuweruzidwa. 14. Ndipo
iwo akaona chizindikiro chochokera kwa Mulungu
amachisandutsa ngati chinthu choseweretsa. 15. Ndipo
amati, "Ichi si china ayi koma matsenga woonekera
poyera." 16. "Chiyani! Ife tikafa ndi kusanduka fumbi ndi
mafupa, kodi tidzaukitsidwa?" 17. "Ndiponso makolo athu
amakedzana?" 18. Nena, "Inde mudzachititsidwa manyazi."
19. Ndipo udzakhala mfuwu umodzi ndipo taona iwo
adzakhala ali kupenyetsetsana. 20. Iwo adzati, "Tsoka kwa
ife! Ili ndi tsiku lachiweruzo." 21. "Ili ndi tsiku lachiweruzo
limene inu mumati ndi bodza." 22. (Kudzanenedwa kuti);
"Bweretsani anthu ochimwa pamodzi ndi anzawo ndi
zinthu zimene iwo anali kupembedza." 23. "Kuonjezera pa
Mulungu weniweni ndipo atsogolereni ku njira ya kumoto."
24. "Ndipo aimitseni. Ndithudi, iwo ayenera kufunsidwa."
25. "Kodi mwatani? Nanga ndi chifukwa chiyani inu simuli
kuthandizana?" 26. Iyayi! Koma iwo lero ndi odzipereka.
27. Ndipo iwo adzafunsana wina ndi mnzake. 28. Iwo
adzati, "Ndinu amene munali kubwera kwa ife kuchokera
kudzanja lamanja." 29. Iwo adzayankha kuti, "Iyayi, Inuyo
simunali okhulupirira." 30. "Ndipo ife tidalibe ulamuliro
pa inu. Iyayi! Inu mudali osamva." 31. "Kotero chiweruzo
cha Ambuye wathu chadza pa ife. Ndithudi tsopano
tidzachilawa." 32. "Choncho ife tidakusocheretsani
chifukwa nafenso tidali osochera." 33. Ndipo, ndithudi,
patsiku limeneli onse adzalandirana chilango pakati pa
wina ndi mnzake. 34. Ndithudi mmenemo ndi mmene
timachitira ndi anthu olakwa. 35. Ndithudi pamene iwo,
adauzidwa kuti, "Kulibe mulungu wina koma Mulungu
weniweni, iwo anali kudzitukumula." 36. Ndipo adanena

kuti, “Kodi ife tisiye milungu yathu chifukwa cha Mlakatuli
wamisala?” 37. Iyayi. Iye wadza ndi choonadi ndipo ali
kutsimikizira uthenga wa Atumwi amene adadza kale.
38. Ndithudi, inu mudzalangidwa kwambiri. 39. Ndipo inu
mudzalandira mphotho molingana ndi ntchito zanu.
40. Kupatula akapolo osankhidwa a Mulungu. 41. Kwa
iwo mphotho yawo ndi yodziwika. 42. Zipatso ndipo iwo
adzalemekezeka kwambiri. 43. M’minda ya chisangalalo.
44. Atakhala pa mipando ya chifumu moyang’anizana.
45. Pakati pawo padzaperekedwa chikho cha vinyo wabwino.
46. Oyera ndiponso okoma kwa iwo amene amamwa.
47. Simudzakhala mavuto mu icho ndipo sichidzawatopetsa.
48. Ndipo pakati pawo padzakhala akazi angwiro opanda
chimasomaso. 49. Okhala ngati mazira osamalidwa bwino.
50. Ndipo adzadza kwa anzawo ndi kumafunsana wina
ndi mnzake. 51. Wina wochokera pakati pawo adzayankhula
nati, “Ndithudi ine ndinali ndi bwenzi langa.” 52. “Amene
amakonda kunena kuti; “Kodi ndiwe mmodzi mwa
okhulupirira?” 53. “Kodi ife tikafa ndi kusanduka dothi ndi
mafupa, tidzatengedwa kupita ku chiweruzo? 54. Iye adati,
“Kodi iwe ungaone pansi?” 55. Motero adayang’ana pansi
ndipo adamuona iye ali pakati pa moto wa ku Gahena.
56. Iye adati, “Pali Mulungu! Iwe udatsala pang’ono
kundipweteka.” 57. “Ndipo kukadapanda chisomo cha
Ambuye wanga ine, ndithudi, ndikadakhala mmodzi wa
iwo.” 58. “Kodi ndiye kuti ife sitidzafa?” 59. “Kupatula kufa
koyamba, kodi ife sitidzalangidwa?” 60. Ndithudi uku
ndiko kupambana kwenikweni. 61. Pofuna kupeza zotere,
alekereni alimbikire amene akufuna kuti alimbikirewo.
62. Kodi chimenechi ndi chabwino kapena mtengo wa

Zaqqum? 63. Ndithudi tazipanga izi kukhala mayesero kwa
anthu olakwa. 64. Ndithudi umenewu ndi mtengo umene
umamera pansi pa Gahena. 65. Zipatso zake zili ngati
mitu ya a Satana. 66. Ndithudi iwo adzadya zimenezi ndi
kukhutitsa mimba zawo ndi zipatsozo. 67. Ndithudi iwo
akadzadya, adzamwa chakumwa chokonzedwa ndi madzi
owira. 68. Ndithudi iwo adzapita ku Gahena. 69. Ndithudi
iwo adapeza makolo awo ali osochera. 70. Kotero iwo ali
kutsatira mapazi awo. 71. Ndithudi makolo awo adasochera
iwo asanadze. 72. Ndipo, ndithudi, ife tidatumiza Atumwi
pakati pawo. 73. Ndipo taona zimene zidadza kwa iwo
amene adachenjezedwa. 74. Kupatula akapolo osankhidwa
a Mulungu omwe ndi anthu olungama.

75. Ndipo ndithudi Nowa adatipempha Ife ndipo Ife
timayankha bwino pa amene amayankha. 76. Ndipo Ife
tidamupulumutsa iye pamodzi ndi banja lake ku chilango
choopsa. 77. Ndipo tidapulumutsanso ana ake. 78. Ndipo
tidakhazikitsa ulemu pa iye pakati pa mitundu yonse
yamtsogolo. 79. Mtendere ukhale kwa Nowa kuchokera
kwa zolengedwa zonse. 80. Ndithudi mmenemo ndi mmene
timalipirira anthu ochita zabwino. 81. Ndithudi iye adali
mmodzi mwa akapolo athu okhulupirira. 82. Ndipo ena
onse tidawamiza.

83. Ndithudi pakati pa iwo amene amatsatira njira yake
adali Abrahamu. 84. Pamene iye adadza kwa Ambuye wake
ndi mtima woyera. 85. Pamene iye adati kwa atate wake
ndi anthu a mtundu wake, “Kodi ndi chiyani chimene inu
muli kupembedza?” 86. “Kodi mukufuna milungu yabodza
kapena Mulungu weniweni?” 87. “Kodi mukuganiza zotani
za Ambuye wa zolengedwa zonse?”

88. Ndipo iye adayang'ana nyenyezi. 89. Ndipo iye adati,
"Ndithudi ndili kudwala." 90. Kotero iwo adamusiya ndi
kubwerera. 91. Ndipo iye adayang'ana kwa milungu yawo nati,
"Kodi inu simudya?" 92. "Kodi bwanji inu simuyankhula?"
93. Ndipo iye adadza pafupi ndi iyo ndi kuigwetsa ndi
dzanja lake lamanja. 94. Nthawi yomweyo wopembedza
mafano adadza kwa iye mwamsangamsanga. 95. Iye adati,
"Kodi mumapembedza zinthu zimene inu mwasema?"
96. "Pamene Mulungu ndiye amene adakulengani
inu pamodzi ndi zosemasema zanuzi!" 97. Iwo adati,
"Mupangireni ng'anjo ndipo muponyeni m'moto woyaka!"
98. Iwo adachita chiwembu koma Ife tidawachititsa
manyazi. 99. Ndipo iye adati, "Ine ndithawira kwa Ambuye
wanga. Ndipo Iye adzanditsogolera ine." 100. "Ambuye
wanga! Ndipatseni ana kuchokera kwa ochita ntchito
zabwino." 101. Ndipo Ife tidamuuza nkhani yabwino ya
mwana wamwamuna wopirira.

102. Ndipo pamene iye adakula mofika pa msinkhu woti
angathe kuthandiza abambo ake, iye adati: "Mwana wanga!
Ndithudi ine ndalota ndili kukupha ngati nsembe. Taganiza
zimene uli kuziona." Iye adati, "Atate wanga! Inu chitani
monga momwe mwalamulidwira. Ngati Mulungu afuna,
mudzandipeza ine wopirira!" 103. Ndipo pamene onse
adadzipereka, ndipo adamugoneka iye chafufumimba.
104. Ndipo Ife tidamuitana ndipo tidati, "Iwe Abrahamu!"
105. "Ndithudi wakwaniritsa maloto ako." Ndithudi
mmenemo ndi mmene timaperekera mphotho kwa
anthu ochita zabwino. 106. Ndithudi awa adali mayesero
oonekeratu. 107. Ndipo tidamupatsa iye nsembe yaikulu.
108. Ndipo Ife tidakhazikitsa ulemu pa iye pakati pa

mibadwo yamtsogolo. 109. Mtendere ukhale pa Abrahamu.
110. Mmenemo ndi mmene timalipira mphotho kwa anthu
ochita zabwino. 111. Ndithudi iye adali mmodzi wa akapolo
athu okhulupirira. 112. Ndipo Ife tidamuuza nkhani yabwino
ya Isake, Mtumwi, wochokera pakati pa anthu okhulupirira.
113. Ndipo Ife tidaika madalitso athu pa iye ndi pa Isake.
Ndipo pakati pa ana awo pali ena ochita ntchito zabwino
ndi ena amene ndi olakwa ndipo amadzipondereza okha.

114. Ndipo, ndithudi, Ife tidaonetsa chisomo chathu
kwa Mose ndi Aroni. 115. Ndipo tidawapulumutsa onse
pamodzi ndi anthu awo ku mavuto oopsa. 116. Ndipo
Ife tidawathandiza kotero adali opambana. 117. Ndipo
Ife tidawapatsa Buku Lopatulika limene limathandiza
kufotokoza zinthu momveka bwino. 118. Ndipo Ife
tidawatsogolera ku njira yoyenera. 119. Ndipo Ife
tidakhazikitsa ulemu kwa iwo pakati pa mibadwo ya
mtsogolo. 120. "Mtendere ukhale pa Mose ndi Aroni."
121. Ndithudi mmenemo ndi mmene timaperekera mphotho
kwa anthu ochita ntchito zabwino. 122. Ndithudi onse adali
akapolo athu okhulupirira.

123. Ndithudi Eliya anali mmodzi wa Atumwi. 124. Pamene,
iye adati kwa anthu ake, "Kodi inu simungaope Mulungu?"
125. "Kodi muli kupembedza Bala ndi kusiya kupembedza
Namalenga?" 126. "Mulungu, Ambuye wanu ndi Ambuye
wa makolo anu akale?" 127. Koma iwo adamukana iye
ndipo ndithudi, iwo adzatengedwa. 128. Kupatula akapolo
osankhidwa a Mulungu, 129. Ndithudi tidakhazikitsa
ulemu kwa iye pakati pa mibadwo ya patsogolo.
130. "Mtendere ukhale ndi Eliya." 131. Ndithudi mmenemo
ndi mmene timaperekera mphotho kwa anthu ochita

ntchito zabwino. 132. Ndithudi iye adali mmodzi wa akopolo
athu okhulupirira.
133. Ndipo Loti adali mmodzi wa Atumwi. 134. Pamene,
Ife tidamupulumutsa iye pamodzi ndi onse omutsatira.
135. Kupatula mayi mmodzi wokalamba amene adali m'gulu
la anthu otsalira m'mbuyo. 136. Ndipo Ife tidawaononga
onse. 137. Ndithudi inu mumawadutsa nthawi ya m'mawa.
138. Ndi nthawi yausiku, kodi inu simungazindikire?
139. Ndipo, ndithudi, Yona adali mmodzi wa Atumwi.
140. Pamene iye adathawa kupita ku chombo chodzadza
kwambiri ndi katundu. 141. Iye adachita nawo mayere
koma iye adali mmodzi wa olephera. 142. Ndipo nsomba
idamumeza iye chifukwa adalakwa. 143. Koma kukadakhala
kuti sadapemphe chikhululukiro cha Mulungu
wolemekezeka 144. Ndithudi iye akadakhalabe m'mimba
mwa nsomba mpaka tsiku la kuuka kwa akufa. 145. Koma
Ife tidakamuponya pa mtunda pamene iye anali kudwala.
146. Ndipo Ife tidameretsa chitsamba cha chipanda kuti
chimere pamwamba pake. 147. Ndipo tidamutumiza kwa
anthu zikwi makumi khumi kapena kuposa apa. 148. Ndipo
onse adakhulupirira ndipo Ife tidawapatsa chisangalalo cha
kanthawi kochepa.
149. Ndipo tsopano afunseni kuti, "Kodi Ambuye wako ali
ndi ana 150. Kapena kuti Ife tidalenga angelo kukhala akazi
pamene iwo anali kuona? 151. Kodi iwo sanena zabodza
pamene amati, 152. "Mulungu wabereka mwana?" Ndithudi
iwo ndi abodza! 153. Kodi iye adasankha ana aakazi m'malo
mwa ana aamuna? 154. Kodi mwatani? Kodi mumaweruza
bwanji? 155. Kodi simungaganize bwino? 156. Kapena kodi inu

muli ndi ulamuliro weniweni? 157. Kotero bweretsani Buku
lanu ngati ndinu olungama!
158. Ndipo iwo akhazikitsa ubale pakati pa Mulungu ndi
majini. Koma majini amadziwa kuti iwo adzatengedwa
kupita kwa Iye. 159. Ulemerero ukhale kwa Mulungu. Iye ali
pamwamba pa zimene amamuyerekeza nazo. 160. Kupatula
akapolo a Mulungu, amene Iye amasankha. 161. Ndithudi
inu pamodzi ndi zimene mupembedza. 162. Simungathe
kusocheza wina aliyense. 163. Kupatula okhawo amene
adzapita ku moto wa ku Gahena. 164. Aliyense wa Ife ali
ndi malo ake ake. 165. Ndithudi ndife amene timaima pa
mizere kupemphera. 166. Ndipo, ndithudi, ndife amene
timamulemekeza.
167. Ndipo, ndithudi, iwo anali kunena kuti;
168. "Tikadakhala ndi chikumbutso monga chomwe chinali
ndi anthu akale." 169. "Ife, ndithudi, tidakhala akapolo
osankhidwa a Mulungu." 170. Koma iwo sakhulupilira
mu izi komabe iwo adzadziwa, 171. Ndithudi mawu athu
adatsogola kwa akapolo athu omwe ndi Atumwi athu.
172. Kuti iwo, ndithudi, adzathandizidwa. 173. Ndipo,
ndithudi, gulu lathu lokha lidzakhala lopambana.
174. Kotero uyambe wawasiya okha kwa kanthawi kochepa.
175. Ndipo uwaone ndipo iwo adzadzioneranso.
176. Kodi iwo afuna kufulumizitsa chilango chathu?
177. Koma pamene icho chidzadza pa iwo, udzakhala
m'mawa woipa kwa iwo amene adachenjezedwa! 178. Kotero
uyambe wawasiya okha kwa kanthawi kochepa. 179. Ndipo
uwaone ndipo nawo adzaona. 180. Ulemerero ukhale kwa
Ambuye wako, Ambuye wolemekezeka ndi wamphamvu,
kuposa zimene ali kumukundikira. 181. Ndipo mtendere

ukhale kwa Atumwi onse. 182. Ndipo kuyamikidwa ndi
kuthokoza konse kukhale kwa Mulungu, Ambuye wa
zolengedwa zonse.

Sura 38 • Sâd

# Al Suad

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni chosatha.

1. Suad.

Pali Korani yodzadza ndi chikumbutso. 2. Iyayi! anthu
osakhulupirira ali kungodzikundikira ndi kumangotsutsa.
3. Kodi ndi mibadwo ingati imene Ife tidaononga iwo
asanadze ndipo iyo idalira poona kuti padalibe nthawi
yothawa?

4. Ndipo iwo ali kudabwa kuti Mtumwi wadza kwa iwo
kuchokera pakati pawo. Ndipo anthu osakhulupirira amati,
"Uyu ndi munthu wamatsenga ndiponso wabodza!" 5. "Kodi
iye wapanga milungu yonse kukhala Mulungu mmodzi?
Ndithudi ichi ndi chinthu chachilendo." 6. Ndipo atsogoleri
awo amachoka monyinyirika nati, "Pitirizani inu ndipo
mudzipereke kwathunthu kwa milungu yanu! Ndithudi
ichi ndi chinthu choti chikusokonezani." 7. "Ife sitidamvepo
zimenezi pakati pa anthu akale. Ichi si china koma nkhani
zopeka chabe." 8. "Kodi uthenga wavumbulutsidwa kwa
iye yekha pakati pathu?" Iyayi! Koma iwo ali kukayika za
uthenga wanga. Iyayi! Iwo sadalawepo chilango changa!

9. Kapena iwo ndi nkhokwe za chifundo cha Ambuye

wako, Mwini Mphamvu zonse, Mwini kupereka zabwino
zonse? 10. Kapena iwo ali ndi ulamuliro kumwamba ndi
padziko ndi kuti zonse zimene zili m'menemo ndi zawo?
Ngati nditero, alekeni iwo kuti akwere mothandizidwa.
11. Iwo adzagonjetsedwa monga magulu akale. 12. Asanadze
iwo, panali ena amene adakana Atumwi. Anthu a Nowa,
a Aad, ndi a Farawo, mfumu ya zisonga. 13. Thamoud ndi
anthu a Loti ndi anthu okhala m'nkhalango, onsewa adali
wothandizana. 14. Panalibe mmodzi amene sadanene kuti
Atumwi adali abodza, motero chilango changa chinali
chowayenera. 15. Ndipo awa ali kungodikira kulira kumodzi
kokha kumene kuchitike mosachedwa. 16. Iwo amati,
"Ambuye wathu, bweretsani msanga kwa ife Buku la
ntchito zathu ngakhale nthawi yake siinakwane."

17. Khala wopirira pa zimene ali kunena ndipo
uzikumbukira kapolo wathu Davide, munthu
wamphamvu. Ndithudi iye anali kulapa nthawi zonse.
18. Ndithudi Ife tidauza mapiri kuti aziyimba pamodzi ndi
iye mayamiko athu nthawi ya madzulo ndi m'mbandakucha.
19. Ndipo mbalame zidasonkhana, zonse pamodzi ndi
iye zidalemekeza Mulungu. 20. Tidalimbikitsa Ufumu
wake ndipo tidamupatsa nzeru ndi kuweruza kwabwino
m'manenedwe ndi m'chiweruzo. 21. Kodi nkhani ya anthu
okangana yakupeza iwe? Pamene, iwo adakwera chipupa
cha nyumba ndi kulowa mnyumba ya padera? 22. Pamene
adalowa kwa Davide, iye adachita mantha ndi iwo ndipo
iwo adati, "Usaope. Ife ndife anthu okangana, ndipo wina
wa ife wachimwira mnzake motero weruza mwachilungamo
ndipo usatiweruze opanda chilungamo koma titsogolere
ku njira yoyenera."

23. “Ndithudi uyu ndi m’bale wanga ndipo ali ndi nkhosa
makumi asanu ndi anayi kudza mphambu zisanu ndi
zinayi pamene ine ndili ndi nkhosa imodzi yokha basi.
Komabe iye akuti, ‘Undipatse ine nkhosayo’ ndipo iye
adandipambana mu zonena zake.” 24. Iye adati, “Ndithudi
iye wakulakwira kwambiri pokupempha kuti nkhosa
yako imodzi yokha iperekedwe kwa iye kuonjezera pa
zimene ali nazo.” Ndithudi anthu ambiri ochitira pamodzi
malonda ndi amene akulakwirana wina ndi mnzake. Koma
izi sizichitika ndi anthu amene amakhulupirira ndipo
amachita ntchito zabwino ndipo anthu otere ndi ochepa.
Ndipo Davide adazindikira kuti Ife tidamuyesa iye ndipo
adapempha chikhululukiro kwa Ambuye wake ndipo iye
adagwa nagunditsa mphumi yake pansi ndi kudza molapa.
25. Kotero Ife tidamukhululukira ndipo ndithudi adali
kufupi ndi Ife ndipo ali ndi malo okongola pa nthawi
yobwerera.

26. Iwe Davide! Ndithudi Ife takukhazika iwe kukhala
Kazembe padziko lapansi motero weruza pakati pa anthu
mwachilungamo, ndipo usatsatire zilakolako za mtima
wako chifukwa zidzakusocheretsa ku njira ya Mulungu.
Ndithudi iwo amene asochera ku njira ya Mulungu
adzalangidwa kwambiri chifukwa iwo amaiwala za tsiku
lachiweruzo.

27. Si kuti tidasowa chochita polenga kumwamba
ndi dziko lapansi ndi zonse zimene zili m’kati mwake!
Amenewo adali maganizo a anthu osakhulupirira! Ndipo
tsoka kwa anthu osakhulupirira lochokera ku moto. 28. Kodi
Ife tingasamale mofanana anthu okhulupirira ndi ochita
ntchito zabwino ndi iwo amene amadzetsa chisokonezo

pa dziko? Kapena Ife tingasamalire anthu amene amalewa
zoipa chimodzimodzi ndi iwo amene amachita zoipa?
29. Ili ndi Buku limene Ife tatumiza kwa iwe, lodzala ndi
madalitso kuti akhoza kuganiza mofatsa pa mavesi ake ndi
kuti anthu ozindikira akhoza kukumbukira.

30. Kwa Davide Ife tidamupatsa Solomoni. Kapolo
wabwino zedi! Ndithudi iye anali kudzalapa kwa Ife.
31. Ndipo pamene adadza nazo kwa iye, nthawi ya
madzulo, Hatchi zophunzitsidwa bwino zamphamvu ndi
zoberekedwa bwino. 32. Ndipo iye adati, "Ndithudi ine
ndidakonda chuma kuposa kukumbukira Ambuye wanga.
Mpaka pamene nthawi idatha ndipo dzuwa lidalowa mu
mdima." 33. Ndipo iye adati "Bweretsani mahatchi kwa ine."
Ndipo iye adayamba kuzisisita miyendo ndi makosi awo.

34. Ndipo, ndithudi, Ife tidamuyesa Solomoni ndipo
Ife tidaika Satana pa mpando wake wachifumu koma iye
adadza kwa Ife modzipereka ndi molapa. 35. Iye adati,
"Ambuye wanga! Khululukireni ndipo ndipatseni ufumu
umene simudzapatsanso wina pambuyo panga chifukwa
inu mumapereka zokoma zanu mopanda muyeso."
36. Ndipo Ife tidamuchepetsera mphamvu yakuti mphepo
imvere malamulo ake kuti iziyenda potsatira malamulo ake
amene iye adalamula. 37. Ndiponso a Satana ochokera kwa
majini ndi m'misiri aliyense womanga nyumba ndi wodziwa
kusambira pa madzi. 38. Ndi ena omwe ndi omangidwa ku
magoli. 39. Iyi ndi mphatso yathu yaulere, kotero pereka
mowolowa manja kapena kuisunga. Iwe siudzaimbidwa
mlandu. 40. Ndipo ndithudi iye adali pafupi ndi Ife, ndi
kubwera ku malo abwino.

41. Ndipo kumbukira kapolo wathu Yobu pamene

adapempha kwa Ambuye wake kuti, “Satana
wandikundikira mavuto ndi masautso.” 42. “Menya nthaka
ndi phazi lako. Uyu ndi kasupe wa madzi oti usambe, ozizira
ndi okoma pakumwa.” 43. Ndipo Ife tidamubwezera banja
lake ndi kuonjezera chiwerengero chawo ngati chisomo
chochokera kwa Ife ndiponso chikumbutso kwa anthu
ozindikira. 44. Ndipo nyamula m’manja mwako mtolo wa
udzu ochepa ndipo mumenye nawo koma usaphwanye
lonjezo lako. Ndithudi! Ife tidamupeza ali wopirira
kwambiri ndi okhazikika. Ndithudi iye adali Mtumwi
wabwino! Ndithudi iye anali kulapa nthawi zonse.

45. Ndipo kumbukira akapolo athu Abrahamu, Isake,
Yakobo amene adali odzala ndi mphamvu ndiponso omvetsa
zinthu za chipembedzo. 46. Ndithudi tidawasankha iwo ndi
kuwapatsa chikumbumtima chamoyo umene uli nkudza.
47. Ndipo iwo timawaona. Ndithudi ali m’gulu la anthu
odziwika ndi abwino. 48. Ndipo kumbukira Ishimayeli,
Elisa, ndi Dhul-Kifl onse adali m’gulu la anthu ochita
zabwino.

49. Ichi ndi chikumbutso, ndithudi, kwa anthu olungama
awo ndi malo abwino. 50. Minda yosatha imene makomo ake
adzakhala otsekulidwa kwa iwo nthawi zonse. 51. M’menemo
iwo adzakhala mwamtendere ndiponso m’menemo iwo
adzaitanitsa zipatso zochuluka ndi zakumwa zokoma.
52. Ndipo pambali pawo padzakhala a namwali angwiro
ongoyang’ana maso awo pa amuna ofanana nawo zaka.
53. Limeneli ndi lonjezo limene lapatsidwa kwa inu lokhudza
tsiku lachiweruzo. 54. Ndithudi zimenezi ndi zokoma zathu
kwa inu ndipo sizidzatha ayi.

55. Izi zili choncho. Ndipo zoonadi anthu ochita zoipa

adzakhala ku malo oipa kupitako. 56. Gahena! Ndi kumene
iwo adzalowa ndipo ndi malo oipa kukhalamo. 57. Izi
zili choncho! Kotero alekeni iwo alawe madzi owira ndi
mafinya. 58. Ndi zilango zina zofanana zawo ndi zina
zosiyanasiyana. 59. Ili ndi gulu la nkhondo limene lili kulowa
ndi inu! Palibe kulandiridwa kwabwino kwa iwo! Ndithudi
iwo adzalowa kumoto! 60. Iwo adzati, "Iyayi! Inunso.
Simulandiridwa ayi. Ndinu amene mudatinyenga ife,
kotero awa ndiwo malo oipa kwambiri kukhalako." 61. Iwo
adzati, "Ambuye wathu! Aliyense amene adachititsa kuti
zimenezi zidze kwa ife muonjezereni kawiri chilango chake
cha kumoto." 62. Ndipo iwo adzati, "Kodi zachitika bwanji
kuti ife sitili kuona anthu amene tinkawawerenga pakati pa
anthu ochita choipa?" 63. Kodi ife timangowanyoza kapena
maso athu alephera kuwaona bwinobwino? 64. Ndithudi
zimenezi ndi zoona. Zokangana za anthu a ku moto.

65. Nena, "Ndithudi ine ndine mchenjezi basi ndipo
kulibe mulungu wina koma Mulungu mmodzi yekha,
wopambama ndi wofunika." 66. "Ambuye wa kumwamba
ndi dziko lapansi ndi zonse zimene zili m'menemo. Iye
ndi wamphamvu zambiri ndi wokhululukira nthawi
zonse." 67. Nena, "Uwu ndi uthenga wofunika kwambiri."
68. "Umene inu muli kuukana." 69. "Ine sindidziwa za mafumu
olemekezeka pamene amatsutsana ndi kukambirana."
70. "Koma akuti ichi chavumbulutsidwa kwa ine kuti ndine
opereka chenjezo lomveka ndiponso poyera."

71. Ndipo pamene Ambuye wako adati kwa Angelo,
"Ndithudi Ine ndidzalenga munthu kuchokera ku dothi."
72. Ndipo ndikatha kumulenga iye ndi kumupumira
mzimu wanga kotero igwani nonse ndi kumulambira

iye. 73. Kotero Angelo onse pamodzi adamulambira.
74. Kupatula Satana, iye anali ndi mwano ndipo iye anali
mmodzi wa osakhulupirira. 75. Mulungu adati, "Iwe Satana!
Chakuletsa ndi chiyani kulambira munthu amene ndalenga
ndi manja anga? Kodi ndiwe wamwano? Kodi kapena iwe
ndiwe mmodzi wa apamwamba?" 76. Iye adati, "Ine ndine
wopambana kuposa iye. Inu mudandilenga ine kuchokera
kumoto pamene iye mudamulenga kuchokera ku dothi."
77. Mulungu adati, "Kotero choka pamaso panga chifukwa
iwe ndiwe okanidwa ndi otembereredwa." 78. "Ndipo
ndithudi matemberero anga adzakhala pa iwe mpaka pa
tsiku lachiweruzo."

79. Satana adati, "Ambuye wanga! Ndipatseni mpata
mpaka patsiku louka kwa akufa." 80. Mulungu adati, "Mpata
waperekedwa kwa iwe." 81. "Mpaka pa nthawi yomwe
idakhazikitsidwa." 82. Satana adati, "Kotero kudzera ku
mphamvu zanu, ine ndidzawasocheretsa." 83. "Kupatula
akapolo anu osankhidwa amene ali pakati pawo."
84. Mulungu adati, "Ichi ndi choonadi ndipo choonadi
ndicho chimene ndimanena." 85. "Kuti ndidzadzadza
Gahena ndi iwe ndiponso onse amene amakutsatira iwe."

86. Nena "Ine sindili kukufunsani malipiro chifukwa
cha ichi ndiponso ine sindine wodziyenereza." 87. "Ichi si
china koma chikumbutso kwa anthu a mitundu yonse."
88. "Ndithudi nonse mudzadziwa choonadi chake nthawi
ina."

# Al Zumar

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Chivumbulutso cha Buku ili ndi chochokera kwa
Mulungu, Mwini mphamvu ndi Mwini nzeru. 2. Ndithudi
tavumbulutsa kwa iwe Buku mwachoonadi. Motero
pembedza Mulungu yekha ndipo udzipereke kwa Iye
kwathunthu. 3. Ndithudi kumvera ndi kupembedza, ndi
kwa Mulungu yekha ndipo iwo amene amasankha ena
kuti akhale owasamala m’malo mwa Mulungu amati, “Ife
sitiwapembedza iwo ayi koma timafuna kuti iwo atifikitse
pafupi ndi Mulungu.” Ndithudi Mulungu adzaweruza
pa zonse zimene iwo amatsutsana. Ndithudi Mulungu
satsogolera wabodza ndi wosakhulupirira.
4. Ngati Mulungu akadafuna kukhala ndi mwana,
ndithudi, Iye akadasankha iwo amene wawafuna kuchokera
ku gulu la zolengedwa zake. Koma ulemerero ukhale kwa
Iye. Iye ndi Mulungu mmodzi ndi wogonjetsa onse. 5. Iye
adalenga kumwamba ndi dziko lapansi m’choonadi Iye
amapanga usiku kuti uphimbe usana ndiponso amapanga
usana kuti uphimbe usiku ndipo adalamula dzuwa ndi
mwezi kukhala zopanda mphamvu. Chilichonse kumaenda
mu msewu wakewake. Ndithudi Iye ndi wamphamvu, ndi
wokhululukira nthawi zonse.
6. Iye adakulengani inu nonse kuchokera kwa munthu
mmodzi ndipo adalenga mnzake wolingana naye. Ndipo

Iye adakutumizirani inu ng'ombe zisanu ndi zitatu zazimuna ndi zazikazi. Iye adakulengani inu m'mimba mwa amayi anu, chilengedwe chotsagana ndi chilengedwe china, m'magulu atatu a mdima. Iye ndiye Mulungu, Ambuye wanu. Kulibenso Mulungu wina koma Iye yekha. Nanga ndi chifukwa chiyani inu musocheretsedwa?

7. Ngati inu simukhulupirira, ndithudi, muyenera kudziwa kuti Mulungu ndi woima payekha ndipo alibe nanu kanthu ayi. Iye sakonda kusakhulupirira kwa akapolo ake. Koma ngati inu muthokoza, Iye amasangalala nanu. Ndipo palibe munthu amene adzasenza katundu wa mnzake. Ndipo ndi kwa Ambuye wanu kumene nonse mudzabwerera. Ndipo Iye adzakuuzani zonse zimene mudachita. Ndithudi Iye amadziwa chilichonse chimene chili m'mitima mwanu.

8. Koma pamene mavuto akhazikika pa munthu, iye amapempha Ambuye wake pafupipafupi koma munthuyo akalandira chisomo chochokera kwa Ambuye wake iye amaiwala zimene amalilira poyamba ndipo amakhazikitsa opikisana ndi Mulungu ndi cholinga chosokoneza anthu ku njira yoyenera ya Mulungu. Nena "Basangalalani ndi kusakhulupirira kwanu kwa kanthawi kochepa. Ndithudi
inu ndinu okakhala ku moto!" 9. Kodi iye amene amamvera
Mulungu ndipo amadzipereka m'mapemphero nthawi ya usiku ndi kugwada kapena kuimirira popembedza ndiponso amene amaopa za m'moyo umene uli nkudza ndipo amalakalaka chisomo cha Ambuye wake ndi wofanana ndi osakhulupirira? Nena, "Kodi iwo amene amadziwa ndi ofanana ndi iwo osadziwa?" Ndi okhawo amene ndi ozindikira amene adzakumbukira.

10. Nena, "Oh inu akapolo anga amene mwakhulupirira!

Opani Ambuye wanu. Mphotho yokoma ili kuwandikira
iwo amene amachita zabwino m'dziko lino. Ndipo dziko la
Mulungu lili ndi malo ambiri. Ndipo onse amene amapirira,
ndithudi adzalandira mphotho yopanda malire."
11. Nena, "Ine ndalamulidwa kuti ndizipembedza Mulungu
ndi mtima wanga wonse." 12. "Ndiponso ine ndalamulidwa
kukhala woyamba pakati pa iwo amene amadzipereka
kwa Mulungu, m'Chisilamu." 13. Nena, "Ndithudi ngati
ine ndikapanda kumvera Ambuye wanga, ine ndimachita
mantha ndi chilango cha tsiku loopsa." 14. Nena, "Ndi
Mulungu yekha amene ine ndimamupembedza ndi mtima
wanga wonse." 15. Motero inu pembedzani aliyense amene
mufuna kuonjezera pa Mulungu. "Ndithudi otayika
ndi iwo amene adzataya miyoyo yawo ndi anthu awo pa
tsiku lachiweruzo. Ndithudi kumeneku ndi kutayika
kwenikweni." 16. Iwo adzakutidwa ndi moto pamwamba
pawo ndi magawo a moto pansi pawo. Ndi chimenechi;
Mulungu amaopseza akapolo ake. "Oh inu akapolo anga
motero opani Ine."
17. Ndipo iwo amene sapembedza mafano ndipo
amatembenukira kwa Mulungu molapa, iwo adzapeza
nkhani zabwino. Kotero auze nkhani yabwino akapolo
anga. 18. Iwo amene amamva mawu anga ndipo adawatsatira,
iwo ndiwo amene Mulungu wawatsogolera ndiponso iwo
ndiwo anthu ozindikira.
19. Kodi iye amene chilango chake chagamulidwa
mwachilungamo ndi wofanana ndi munthu wochimwa?
Kodi iwe ungamupulumutse iye amene ali m'moto?
20. Koma iwo amene aopa Ambuye wawo ali ndi nyumba
zokongola ndi zosanjikizana zimene zamangidwa ndipo

pansi pake pamayenda mitsinje. Limeneli ndilo lonjezo la Mulungu ndipo Iye saphwanya lonjezo lake.

21. Kodi inu simuona mmene Mulungu amatumizira mvula kuchokera kumwamba ndipo amaisiya kuti ilowe pansi m'mitsinje? Mmene Iye amameretsera mbewu za maonekedwe osiyanasiyana zimene zimafota ndipo inu mumaziona zitasanduka zachikasu ndipo amazipanga izo kuti ziume ndi kuthetheka? Ndithudi mu zimenezi muli
chikumbutso kwa anthu ozindikira. 22. Kodi iye amene
Mulungu watsekula mtima wake kuti alowe Chisilamu ndi kuona kuwala kochokera kwa Ambuye wake ndi wofanana ndi munthu wouma mtima? Iyayi! Tsoka kwa iwo amene mitima yawo ndi yolimba pokumbukira Mulungu. Ndipo iwo ndi olakwa kwambiri.

23. Mulungu watumiza uthenga wabwino, Buku limene limabwerezabwereza chiphunzitso chake mosiyanasiyana. Matupi a iwo amene amaopa Ambuye wawo, amanjenjemera ndi Bukulo. Ndipo makungu ndi mitima yawo imafewa akamakumbukira Mulungu. Chimenechi ndicho chi langizo cha Mulungu. Iye amatsogolera ndi icho aliyense amene Iye wamufuna. Koma iye amene Mulungu amamusiya kuti asochere, alibe wina woti angamutsogolere.

24. Kodi iye amene adzapanga nkhope yake kukhala chishango cha chilango chowawa cha tsiku louka kwa akufa adzakhala wofanana ndi iye amene wapulumuka? Ndipo zidzanenedwa kwa anthu ochimwa kuti, "Lawani zipatso za
ntchito zanu." 25. Iwo amene adalipo kale nawonso adakana
kotero chilango chidadza pa iwo kuchokera kumbali
imene iwo sanali kuyembekezera. 26. Kotero Mulungu

adawachititsa manyazi m'moyo uno koma chilango cha
m'moyo umene uli nkudza ndi chachikulu iwo akadadziwa!
27. Ndipo Ife tawaikira anthu, m'Buku la Korani, fanizo
la mtundu uliwonse ndi cholinga chakuti azikumbukira.
28. Korani ya chiyankhulo cha Chiarabu, ndipo mulibe
zinthu zolakwa, kuti iwo akhoza kulewa zoipa zimene
Mulungu wawalamula. 29. Mulungu ali kupereka fanizo la
kapolo amene ali ndi mabwana ambiri ndi kapolo amene ali
ndi bwana mmodzi yekha. Kodi anthu awiriwa ndi ofanana
m'machitidwe awo? Ulemerero ukhale kwa Mulungu!
Koma anthu ambiri sadziwa. 30. Ndithudi iwe udzafa
ndipo iwo adzafa. 31. Ndipo patsiku louka kwa akufa, nonse
mudzatsutsana wina ndi mnzake pamaso pa Ambuye wanu.
32. Kodi wolakwa kwambiri ndani kuposa iye amene
amapeka bodza lokhudza Mulungu ndipo amakana
choonadi pamene chidza kwa iye? Kodi ku Gahena kulibe
malo okhalamo anthu osakhulupirira? 33. Ndipo iye amene
wabweretsa choonadi ndi amene adakhulupirira choonadi,
ndithudi, amenewa ndiwo amene amachita bwino. 34. Iwo
adzapeza zonse zimene afuna kuchokera kwa Ambuye
wawo. Imeneyi ndiyo mphotho ya anthu abwino. 35. Kuti
Mulungu adzawakhululukira zoipitsitsa zimene amachita
ndi kuwapatsa mphotho yawo molingana ndi ntchito zawo
zabwino zimene adachita.
36. Kodi Mulungu sakwana kuthandiza akapolo ake?
Komabe iwo amayesetsa kukuopseza ndi milungu ina
yoonjezera pa Iye. Ndipo aliyense amene Mulungu
amusocheza alibe wina womutsogolera 37. Ndipo iye
amene Mulungu amamutsogolera palibe wina amene

angamusocheze. Kodi Mulungu si wamphamvu zambiri
ndiponso Ambuye wodziwa kubwezera?
38. Ndipo, ndithudi, ngati ungawafunse kuti, “Kodi ndani
adalenga kumwamba ndi dziko lapansi?” Ndithudi iwo
adzayankha kuti, “Ndi Mulungu.” Nena, “Kodi zinthu
zimene mumapembedza m’malo mwa Mulungu, ngati
Mulungu afuna kugwetsa mavuto pa ine, kodi zinthuzo
zingathe kuchotsa mavutowo? Kapena ngati Iye alangiza
chisomo chake pa ine, kodi izo zingakanize chisomo
chake?” Nena, “Mulungu ndi wokwana kwa ine. Mwa Iye
onse okhulupirira ayenera kuika chikhulupiriro chawo.”
39. Nena, “Oh inu anthu anga! Gwirani ntchito yanu ndipo
ine ndigwira yanga, ndipo inu mudzadziwa.” 40. Iye amene
alandira chilango chochititsa manyazi ndi iye amene
alandira chilango chamuyaya. 41. Ndithudi tavumbulutsa
kwa iwe Buku la ulangizi kwa anthu mwachoonadi. Kotero
aliyense amene atsatira njira yoyenera amapulumutsa
mzimu wake ndipo aliyense amene asochera alanga mzimu
wake. Ndipo iwe sindiwe msungi wawo ayi.
42. Ndi Mulungu amene amachotsa mizimu ya anthu pa
nthawi ya imfa ndi mizimu ya anthu a moyo akamagona.
Iye amasunga mizimu ya amene adalamula kuti afe ndi
kubweza mizimu ya ena mpaka nthawi yawo itakwana.
Ndithudi mu zimenezi muli zizindikiro kwa iwo amene
amaganiza kwambiri.
43. Kodi iwo asankha ena ngati a mkhalapakati poonjezera
pa Mulungu? Nena, “Ngakhale kuti iwo alibe mphamvu
iliyonse ndiponso alibe nzeru?” 44. Nena “Mphamvu
zonse za mkhalapakati zili m’manja mwa Mulungu. Iye
ndiye Mwini wa chilichonse chimene chili kumwamba

ndi pa dziko lapansi. Ndipo ndi kwa Iye kumene
mudzabwerera.” 45. Ndipo pamene dzina la Mulungu
lokha litchulidwa, mitima ya iwo amene sakhulupirira za
m’moyo umene uli nkudza imakhumudwa koma pamene
milungu ina kupatula Mulungu weniweni itchulidwa,
iwo amasangalala kwambiri! 46. Nena, “Oh Mulungu!
Namalenga wakumwamba ndi dziko lapansi, Wodziwa
zobisika ndi zooneka! Inu mudzaweruza pakati pa akapolo
anu pa zimene amatsutsana.” 47. Ngakhale anthu ochita
zoipa akadakhala ndi zinthu zonse zimene zili pa dziko
lapansi kapena zochuluka kuonjezera pa izi, ndithudi
iwo akadazipereka izo ngati dipo kuti ziwapulumutse ku
zowawa za chilango cha tsiku lachiweruzo. Ndipo chimene
samachiganizira, chidzasonyezedwa kwa iwo ndi Mulungu.
48. Mphotho za ntchito zawo zonse zoipa zidzaonekera
poyera ndipo zonse zimene amazinyoza zidzawazungulira
iwo.

49. Pamene vuto ligwa pa munthu, iye amatipempha Ife,
koma pamene timuonetsa chifundo chathu, iye amati,
“Izi zapatsidwa kwa ine chifukwa cha nzeru zanga.” Iyayi!
Awa ndi mayesero chabe koma ambiri a iwo sadziwa
chilichonse. 50. Ndithudi iwo amene adalipo kale anali
kunena chimodzimodzi koma chilichonse chimene anali
kuchita chidali chopanda phindu kwa iwo. 51. Motero zoipa
zimene adachita zidawatsata iwo. Ndipo iwo ochita zoipa
a m’badwo uno zotsatira za ntchito zawo zidzawapeza
ndipo iwo sadzatha kuthawa ayi! 52. Kodi iwo sadziwa kuti
Mulungu amapereka moolowa manja kapena monyalapsa
kwa aliyense amene Iye wamufuna? Ndithudi mu zimenezi
muli zizindikiro kwa iwo amene ama amakhulupirira.

53. Nena, “Oh akapolo anga amene mwalakwira mizimu yanu! Musakayike za chisomo cha Mulungu. Ndithudi Mulungu amakhulululukira machimo onse. Ndithudi Iye amakhulululukira nthawi zonse ndipo ndiye Mwini chisoni chosatha.” 54. Lapani kwa Ambuye wanu nthawi ndi nthawi ndipo mudzipereke kwathunthu kwa Iye chilango chisanadze kwa inu chifukwa sipadzakhala wina wothandiza inu.

55. Ndipo tsatirani zabwino zonse zimene zavumbulutsidwa kwa inu kuchokera kwa Ambuye wanu chilango chake chisanadze kwa inu mwadzidzidzi pamene inu simuli kuchiganizira. 56. Mwina mzimu ungadzanene kuti, “Oh tsoka kwa ine chifukwa chakulephera kwanga pokwaniritsa udindo wanga kwa Mulungu! Ndithudi ine ndidali mmodzi wa iwo amene anali kunyoza.” 57. Kapena akhoza kunena kuti, “Akadakhala kuti Mulungu adanditsogolera, ndithudi, ine ndikadakhala m’gulu la anthu angwiro.” 58. Kapena pamene aona akhoza kunena chilango kuti, “N’kadakhala ndidali ndi mwayi wina, ndithudi, ndikadakhala m’gulu la iwo ochita zabwino.” 59. Inde! Ndithudi ulangizi wanga unadza kwa inu koma inu munaukana. Inu munali kunyada ndipo munali m’gulu la anthu osakhulupirira. 60. Ndipo patsiku louka kwa akufa, iwe udzaona nkhope zonse za amene amanamizira Mulungu, zitadetsedwa. Kodi ku Gahena kulibe malo okhalako anthu a mwano? 61. Ndipo Mulungu adzapereka onse amene amalewa zoipa ku malo awo opambana. Palibe choipa chimene chidzagwa pa iwo, ndipo iwo sadzamva chisoni ayi.

62. Mulungu ndiye Namalenga wa zinthu zonse, Wosamalira ndiponso Mgawi wa zinthu zonse. 63. Chake

ndi chuma chonse cha kumwamba ndi cha padziko lapansi.
Ndipo iwo amene sakhulupirira muchivumbulutso cha
Mulungu, amenewo ndiwo amene adzakhala olephera.
64. Nena, “Kodi inu muli kundilamula kuti ndipembedze
wina wake osati Mulungu? Oh inu anthu osadziwa!”
65. Ndipo, ndithudi, zavumbulutsidwa kwa iwe ndi kwa iwo
amene adalipo kale kuti, “Ndithudi ngati inu muphatikiza
Mulungu ndi china chake, ndithudi, ntchito zanu
zidzakhala zopanda phindu. Ndithudi inu mudzakhala
m’gulu la anthu olephera.” 66. Iyayi! Koma iwe upembedze
Mulungu m’modzi yekha ndipo khala m’gulu la iwo amene
amathokoza.

67. Ndipo iwo sadamulemekeze Mulungu ndi ulemu
umene uli woyenera kwa Iye ndipo dziko lapansi lidzakhala
pa chikhato pake pa tsiku lachiweruzo. Kumwamba
kudzakulungidwa m’dzanja lake lamanja. Ulemerero
ukhale kwa Iye ndipo Iye ndi woposa mafano amene
amamufanizira nawo! 68. Ndipo lipenga lidzalizidwa kotero
onse amene ali kumwamba ndi onse amene ali padziko
lapansi adzakomoka kupatula okhawo amene Mulungu
wawafuna. Ndipo lidzalizidwanso kachiwiri ndipo onse
adzakhala choimirira ndi kumangoyembekezera. 69. Ndipo
dziko lapansi lidzawala ndi muuni wa Ambuye wako ndipo
Buku lidzatsekulidwa. Atumwi ndi mboni zidzaitanidwa
ndipo chiweruzo chidzaperekedwa mwachilungamo pakati
pawo ndipo iwo sadzaponderezedwa konse. 70. Ndipo
mzimu uliwonse udzalipidwa mokwanira molingana ndi
zimene udachita ndipo Iye amadziwa bwino zonse zimene
mumachita.

71. Ndipo onse osakhulupirira adzatengedwa paulendo

wa ku Gahena m'magulumagulu ndipo pamene azidzafika
pafupi, makomo ake adzatsekulidwa ndipo oyang'anira
kumeneko adzati kwa iwo, "Kodi sikunadze kwa inu
Atumwi a mtundu wanu kukulalikirani ulangizi wa Ambuye
wanu ndi kukuchenjezani za kukumana kwanu ndi tsiku
lino?" Iwo adzati, "Inde!" Koma chilango chakwaniritsidwa
kwa anthu osakhulupirira. 72. Iwo adzauzidwa kuti, "Lowani
nonse m'zipata za Gahena kuti muzikhala m'menemo."
Ndipo ndi oipa malowa womwe anthu onyada adzakhaleko!
73. Ndipo onse amene amaopa Ambuye wawo
adzatsogozedwa ku Paradiso m'magulumagulu. Ndipo
pamene iwo azidzafika pafupi, taonani makomo azipata
adzatsekulidwa, ndipo oyang'anira kumeneko adzati,
"Mtendere ukhale kwa inu!" Inu mudzakhala mosangalala
kotero lowani kuti muzikhala momwemo." 74. Ndipo
iwo adzati, "Ulemerero ukhale kwa Mulungu amene
wakwaniritsa kwa ife lonjezo lake ndipo watilola ife kuti
tikhale m'dziko ili. Ife tidzakhala m'minda imene tifuna."
Kotero yabwino ndi mphotho ya anthu ogwira ntchito
zabwino. 75. Ndipo iwe udzaona angelo atazungulira
Mpando Wachifumu mbali zonse, ali kuimba mayamiko
ndi kulemekeza Ambuye wawo. Ndipo chiweruzo
chidzaperekedwa kwa zolengedwa zonse mwachilungamo
ndipo kudzanenedwa kuti, "Kuyamikidwa konse ndi kwa
Mulungu, Ambuye wa zolengedwa zonse."

# MU-MIN

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. *Ha-Mim.*

2. Chivumbulutso cha Buku ili ndi chochokera kwa
Mulungu, wamphamvu ndi wodziwa zonse. 3. Iye ndi amene
amakhulukira machimo ndipo amavomera kulapa. Iye
ndi wankhanza popereka chilango ndi Mwini chinthu
chilichonse, ndipo kulibe mulungu wina koma Iye yekha.
Kwa Iye chilichonse chidzabwerera.
4. Palibe amene amatsutsa chivumbulutso cha
Mulungu kupatula okhawo amene sakhulupirira. Kotero
usanyengedwe ndi kuyendayenda kwawo kwa m'mizinda.
5. Anthu a Nowa ndi anthu a magulu ena amene adadza
pambuyo pawo adakana Atumwi, ndipo mtundu uliwonse
udachita chiwembu pa Mtumwi wawo, kuti amugwire
kotero anali kutsutsana naye pa zinthu zabodza ndi cholinga
choletsa choonadi. Koma Ine ndidawaononga iwo! Kodi
chilango changa chidali chowawa bwanji? 6. Kotero mawu a
Ambuye wako adakwaniritsidwa kwa osakhulupirira ndipo
iwo ndi amene adzakhala ku Moto!
7. Iwo amene amasunga Mpando Wachifumu ndiponso
iwo amene amauzungulira iwo, amatamanda Ambuye wawo
ndi kukhulupirira mwa Iye ndipo amapempha chitetezo
m'malo mwa iwo amene akhulupirira. "Ambuye wathu!
Chifundo ndi nzeru zanu zimakhudza aliyense kotero

atetezeni onse amene adza kwa Inu ndi kutsatira njira yanu
ndiponso apulumutseni iwo ku chilango cha ku Gahena!"
8. "Ambuye wathu! Alowetseni ku minda ya Paradiso imene
inu mudawalonjeza iwo ndiponso iwo amene amachita
zabwino, pakati pa atate, akazi ndi ana awo. Ndithudi
Inu ndinu wamphamvu ndi wanzeru kwambiri. 9. "Ndipo
apulumutseni ku ntchito zoipa. Aliyense amene Inu
mumupulumutsa ku zoipa tsiku lalero ndiye kuti Inu
mwamuonetsa chisoni chanu ndipo kumeneko ndiko
kupambana kwambiri.

10. Ndithudi iwo amene sakhulupirira adzamva mkuwo
ukuti, "Ndithudi mkwiyo wa Mulungu pa inu ndi waukulu
kuposa chidani chimene inuyo mumadzionetsera nokha
poona kuti munali kuitanidwa kuti mukhulupirire koma
inu munali kukana." 11. Iwo adzati, "Ambuye wathu
mudatipha kawiri konse ndipo mudatipatsa moyo
kawiri. Tsopano ife tivomereza kuchimwa kwathu. Kodi
sitingathe kupulumutsidwa ku chilango cha ku Moto?"
12. "Ichi ndi chifukwa chakuti pamene dzina la Mulungu
lokha linali kupembedzedwa, inu simudakhulupirire
koma pamene milungu ina inali kupembedzedwa, inu
mudakhulupirira. Kotero Mwini wake wa chiweruzo ndi
Mulungu Wapamwamba ndi Wamkulukulu."

13. Iye ndiye amene amakulangizani inu zizindikiro
zake ndipo amakutumizirani chakudya kuchokera ku
mitambo. Koma okhawo amene akumbukira ndiwo amene
amabwerera kwa Mulungu. 14. Motero pembedzani Mulungu
mmodzi yekha, ngakhale kuti anthu osakhulupirira
sasangalala. 15. Wokweza maudindo anthu okhulupirira ndi
Mwini Mpando wachifumu. Iye amatumiza chikumbutso

chake kwa aliyense wa akapolo ake amene Iye wamufuna
kuti akhoza kuchenjeza anthu za tsiku lachiweruzo.
16. Tsiku limene onse adzadza pamodzi, sipadzakhala china
chilichonse chobisika kwa Mulungu. Kodi ndani adzakhala
ndi ulamuliro wamphamvu pa tsikuli? Ndi Mulungu,
mmodzi yekha, Mwini mphamvu zonse. 17. Tsiku limeneli,
mzimu uliwonse udzalandira malipiro ake. Pa tsiku
limeneli sikudzakhala kuponderezana. Ndithudi Mulungu
ndi wachangu pobwezera.

18. Achenjeze iwo za tsiku limene lili pafupi kudza,
limene mitima idzadza mpaka pakhosi ndi kuwakomola.
Palibe bwenzi la pamtima kapena mkhalapakati wa anthu
ochita zoipa amene adzayankhulire. 19. Mulungu amadziwa
chinyengo cha maso ndi zimene mitima imabisa. 20. Ndipo
Mulungu amaweruza mwachilungamo pamene iwo amene
amapembedzedwa oonjezera pa Iye sangathe kuweruza.
Ndithudi Mulungu amamva ndiponso amaona.

21. Kodi iwo sadayende pa dziko lapansi ndi kuona zimene
zidawachitikira anthu a makedzana? Iwo adali a mphamvu
kuposa awa. Koma Mulungu adawalanga chifukwa cha
zoipa zawo. Ndipo iwo adalibe wina aliyense wowateteza
kwa Mulungu. 22. Ichi ndi chifukwa chakuti Atumwi awo
adadza kwa iwo ndi zizindikiro zooneka ndi maso koma
iwo adakana Atumwiwo. Kotero Mulungu adawaononga
iwo. Ndithudi! Iye ndi Wamphamvu ndipo chilango chake
ndi chowawa kwambiri.

23. Ndipo, ndithudi, tidamutumiza Mose ndi uthenga
wathu ndi ulamuliro wooneka. 24. Kwa Farawo, Hamani
ndi Karuni koma iwo adati, “Munthu wamatsenga ndi
wabodza.” 25. Ndipo pamene iye adawauza choonadi

chochokera kwa Ife, iwo adati, "Iphani ana onse aamuna a
anthu amene akhulupirira ndi iye ndipo musunge ana awo
aakazi." Koma ziwembu za anthu osakhulupirira sizitha
bwino chifukwa zilibe maziko enieni.
26. Ndipo Farawo adati, "Mundisiye ine kuti ndiphe Mose
ndipo musiyeni iye kuti apemphe kwa Ambuye wake.
Ndithudi ine ndiopa kuti iye adzasintha chipembedzo
chanu ndi kuyambitsa chisokonezo m'dziko." 27. Ndipo
Mose adati, "Ndithudi ine ndithawira kwa Ambuye wanga
ndi Ambuye wanu kuti anditeteze kwa aliyense wamwano
amene sakhulupirira mu tsiku lachiweruzo."
28. Ndipo munthu wamwamuna wokhulupirira wa m'gulu
la anthu a Farawo amene adabisa chikhulupiriro chake
adati, "Kodi inu mudzapha munthu chifukwa chakuti
wanena kuti Ambuye wanga ndi Mulungu pamene iye
wadza kwa inu ndi zizindikiro zooneka zochokera kwa
Ambuye wanu? Ndipo ngati iye ndi wabodza tchimo
likhale pa iye yekha koma ngati iye ali kunena zoona,
tsoka limene anena lidzagwa pa inu. Ndithudi Mulungu
satsogolera munthu woswa malamulo ndi wabodza."
29. "Oh inu anthu anga! Wanu ndi ufumu walero. Inu muli ndi
ulamuliro m'dziko koma ndani amene adzatithandiza ife ku
chilango cha Mulungu ngati icho chitagwa pa ife?" Farawo
adati, "Ine ndili kungokuuzani zinthu zimene ndimaona
ndiponso ndili kukutsogolerani ku njira yoyenera."
30. Ndipo iye amene adakhulupirira adati, "Oh anthu
anga! Ndithudi ine ndili kuopa kuti inu mudzaona zimene
zidadza pa anthu akale." 31. "Monga zimene zidadza kwa
anthu a Nowa, a Aad ndi a Thamoud ndi iwo amene
adadza iwo atachoka. Koma Mulungu safuna kupondereza

akapolo ake.” 32. “Oh inu anthu anga! Ine ndichita mantha
pa zimene zidzaoneka kwa inu pa tsiku louka kwa akufa.”
33. Tsiku limene inu mudzabwerera ndi kuthawa. Inu
simudzakhala ndi wokutetezani kwa Mulungu. Ndipo
aliyense amene Mulungu amusiya kuti asochere palibe
wina amene angamutsogolere.

34. Ndithudi Yosefe adadza kwa inu ndi zizindikiro
zooneka, koma inu munali kukayika pa zimene iye
adabweretsa mpaka pamene iye adafa ndipo inu mudati,
“Mulungu sadzadzutsanso Mtumwi wina pambuyo pa iye.
Mmenemo ndi mmene Mulungu amamusocheretsa munthu
woononga ndi okayika. 35. Iwo amene amakana uthenga wa
Mulungu popanda ulamuliro umene udapatsidwa kwa iwo,
zochita zawo ndi zodedwa pamaso pa Mulungu ndi pamaso
pa iwo okhulupirira. Mmenemo ndi mmene Mulungu
amaphimbira mtima wa munthu wonyada ndi wamwano.

36. Ndipo Farawo adati, “Oh Hamani! ndimangire
nsanja kuti ndikwere.” 37. “Ndikwere kuti ndikafike
kumwamba kuti ndimpeze Mulungu wa Mose koma ine,
ndithudi, ndiganiza kuti iye ndi wonama.” Kotero ntchito
zoipa za Farao zidaoneka zomusangalatsa, ndipo iye
adasocheretsedwa ku njira yoyenera ndipo zochita zake
sizinamuthandize china chilichonse ayi koma chionongeko.

38. Ndipo iye amene adakhulupirira adati, “Oh inu anthu
anga! Nditsateni ine. Ine ndidzakutsogolerani ku njira
yabwino.” 39. “Oh inu anthu anga! Moyo wa pa dziko lino
ndi chisangalalo cha kanthawi kochepa ndipo, ndithudi,
moyo umene uli nkudza ndi wosatha.” 40. Aliyense amene
achita zoipa adzalandira dipo loipa ndipo aliyense amene
achita zabwino kaya ndi wamwamuna kapena wamkazi

ndipo ndi wokhulupirira, otere adzalowa ku Paradiso
kumene adzapatsidwa madalitso opanda muyeso. 41. “Oh
inu anthu anga! Kodi mwatani! Ine ndili kukuitanirani
ku chipulumutso ndipo inu muli kundiitanira ku moto?”
42. “Inu muli kundiitana kuti ndisakhulupirire mwa
Mulungu ndipo kuti ndizimufanizira Iye ndi zinthu zina
zimene sindizidziwa pamene ine ndili kukuitanani kuti
mudze kwa Mwini mphamvu ndi Mwini chikhululukiro.”
43. “Mosakayika chimene muli kundiitanira chilibe dzina
m’dziko lino ndi m’dziko limene lili nkudza ndipo kuti
tidzabwera kwa Mulungu. Ndipo onse oswa malamulo, malo
awo adzakhala ku moto.” 44. “Ndipo inu mudzakumbukira
zimene ndili kukuuzani ndipo ine ndiika chikhulupiriro
changa mwa Mulungu. Ndithudi Mulungu amaona akapolo
ake.”

45. Kotero Mulungu adamuteteza ku chiwembu chimene
iwo adakonza ndipo anthu a Farawo chilango chonyansa
chidawagwera. 46. Ku moto iwo adzasonkhanitsidwa
m’mawa ndi madzulo ndipo chiweruzo chawo
chidzagamulidwa pa tsiku limene ola lidzakwaniritsidwa
ndi kuti, “Alangeni kwambiri anthu a Farawo.”

47. Ndipo pamene iwo adzakangana wina ndi mnzake
ku moto, anthu ochepa mphamvu adzati kwa iwo amene
anali kuchita mwano, “Ndithudi ife tidali otsatira anu.
Kodi simungatichotserepo chilango cha moto?” 48. Iwo
amene adali a mwano adzati, “Tonse tili kumoto. Zoonadi
Mulungu waweruza pakati pa akapolo ake.” 49. Ndipo
iwo amene adzakhala kumoto adzati kwa iwo osunga
Gahena, “Pemphani kwa Ambuye wanu kuti atichepetsere
chilango chathu tsiku limodzi.” 50. Iwo adzati, “Kodi kwa

inu sikudabwere Atumwi anu ndi zizindikiro zooneka?”
Iwo adzayankha kuti, “Inde.” Ndipo iwo adzati, “Kotero
pemphani ngati mufuna koma pemphero la iwo amene
alibe chikhulupiriro ndi lopanda pake.”

51. Ndithudi Ife tidzapambanitsa Atumwi athu pamodzi
ndi iwo amene amakhulupirira m’dziko lino ndi tsiku limene
mboni zidzaitanidwa. 52. Tsikuli ndi limene madandaulo a
anthu ochita zoipa adzakhala opanda ntchito. Ndipoiwo
adzakhala kumalo oipa. 53. Ndipo Ife, ndithudi ,tidamupatsa
Mose langizo. Ndipo tidapereka Buku loti lisungidwe ndi
ana a Israyeli. 54. Ma langizo ndi chikumbutso kwa anthu
ozindikira. 55. Kotero pirira. Ndithudi lonjezo la Mulungu
ndi loona. Ndipo pempha chikhululukiro cha machimo
ako ndipo lemekeza Ambuye wako madzulo ndi m’mawa.

56. Ndithudi iwo amene amatsutsa mawu a Mulungu
wopanda lamulo limene ladza kwa iwo, alibe china
chilichonse m’mitima mwawo kupatula chilakolako choti
akhale a pamwamba koma iwo sadzakhala. Kotero funafuna
chitetezo cha Mulungu. Ndithudi Iye amamva ndipo
amaona. 57. Ndithudi chilengedwe cha kumwamba ndi
dziko lapansi ndi choposa chilengedwe cha anthu. Koma
anthu ambiri sadziwa. 58. Ndithudi anthu a khungu ndi
anthu openya siofanana ndiponso amene akhulupirira ndi
kuchita ntchito zabwino ndi anthu ochita zoipa (safanana).
Ndi zochepa zomwe mumakumbukira. 59. Ndithudi ola
lidzadza, mosakayika, koma anthu ambiri sakhulupirira.

60. Ndipo Ambuye wako adati, “Ndipempheni Ine ndipo
ndidzayankha pemphero lanu. Ndithudi! Koma iwo amene
ndi amwano pondipembedza Ine, ndithudi, adzaponyedwa
ku Gahena mochititsa manyazi.” 61. Ndi Mulungu amene

adalenga usiku kuti inu muzipumula ndi usana kuti
ukupatseni kuwala. Ndithudi Mulungu amaonetsa chisomo
chake kwa anthu koma anthu ambiri sathokoza ayi.
62. Ameneyu ndiye Mulungu, Ambuye wanu, Namalenga
wa zinthu zonse. Kulibe Mulungu wina koma Iye yekha.
Nanga ndi chifukwa chiyani inu mumanyengedwa ndi
kusiya choonadi? 63. Mmenemo ndi mmene adasiyira
choonadi iwo amene adakana uthenga wa Mulungu.

64. Ndi Mulungu amene adalenga dziko lapansi kukhala
malo anu okhalamo ndi mtambo ngati chotchinga. Iye
ndiye amene adaumba matupi anu ndipo adawaumba
ndi maonekedwe abwino ndipo wakupatsani inu zinthu
zabwino. Ameneyu ndiye Mulungu, Ambuye wanu.
Ulemerero ukhale kwa Mulungu, Ambuye wa zolengedwa
zonse. 65. Iye ndi Wamuyaya. Kulibe Mulungu wina
koma Iye yekha. Mupempheni Iye ndipo mudzipereke
kwathunthu kwa Iye yekha. Ulemerero wonse ukhale kwa
Mulungu, Ambuye wa zolengedwa zonse.

66. Nena, "Ine ndinaletsedwa kupembedza iwo amene inu
mumapembedza kuonjezera pa Mulungu weniweni pamene
malangizo abwino anadza kwa ine kuchokera kwa Ambuye
wanga. Ndipo ine ndalamulidwa kuti ndizimvera Ambuye
wa zolengedwa zonse. 67. Ndiye amene adakulengani inu
kuchokera ku dothi ndipo kuchokera ku dontho la umuna
losakanizana ndi ukazi ndi kuchokera ku magazi oundana
ndipo amakutulutsani kukhala mwana ndipo amakukuzani
kufika pa msinkhu wanu ndi kukhala wamphamvu, ndipo
Iye amakukalambitsani. Ngakhale ena a inu amafa msanga,
Iye amakusiyani inu kuti mufike patsiku loikidwa kuti
mukhoza kuzindikira. 68. Iye ndiye amene amapereka moyo

ndi imfa ndipo pamene Iye afuna chinthu, Iye amangonena
kwa icho kuti, “Khala” ndipo chimakhala.

69. Kodi siudawaone iwo amene amatsutsa uthenga wa
Mulungu? Kodi iwo amabwezedwa bwanji ku choonadi?
70. Iwo amene amakana Buku ndi uthenga umene
tidatumiza ndi Atumwi athu, koma posachedwapa iwo
adzadziwa. 71. Pamene magoli ndi unyolo udzakhala pa
khosi pawo, iwo adzaduduluzidwa 72. M’madzi owira ndipo
iwo adzatenthedwa ku moto. 73. Ndipo zidzanenedwa kwa
iwo, “Kodi zili kuti izo zimene munali kuzipembedza?”
74. “Poonjezera Mulungu?” Iwo adzati, “Zatithawira.
Iyayi ife sitimapembedza zina zake.” Kotero Mulungu
amasocheretsa anthu osakhulupirira. 75. Ichi ndi chifukwa
chakuti inu munali kusangalala ndi zinthu zachabechabe
padziko ndipo munali ndi mwano. 76. Lowani m’zipata za
ku Gahena kuti mukhale m’menemo. Iwowo ndi malo oipa
omwe anthu onyada adzakhaleko.

77. Kotero pirira. Ndithudi lonjezo la Mulungu ndi loona.
Kaya tikuonetsa gawo la zimene tili kuwaopseza nazo
kapena tikupha, komatu kwa Ife iwo adzabwerera.

78. Ndithudi Ife tidatumiza Atumwi iwe usanabadwe.
Alipo ena amene takuuza za iwo ndipo alipo ena amene
sitidakuuze za iwo ndipo sichidali choyenera kuti Mtumwi
abweretse chizindikiro kupatula ndi chilolezo cha
Mulungu. Koma pamene ulamuliro wa Mulungu udadza,
chiweruzo chidaperekedwa mwachilungamo. Ndipo onse,
amene ankati ndi zabodza, adatayika.

79. Mulungu ndiye amene adakulengerani nyama kuti
mukhoza kukwera zina za izo ndi kudya zina za izo.
80. Ndipo muli zambiri zabwino mu nyamazo kuti inu

mukhoza kukwaniritsa zofuna zanu zimene zili m'mitima
mwanu. Ndipo pa izo ndi m'masitima inu mumanyamulidwa.
81. Ndipo Iye amakuonetsani zizindikiro zake. Kodi ndi ziti
za zizindikiro za Mulungu zimene mumakana?
82. Kodi inu simudayende m'dziko ndi kuona zimene
zidawachitikira anthu ena amene adalipo iwo asanabadwe?
Iwo adali ambiri kuposa awa ndipo adali ndi mphamvu
zambiri. Ndipo mwa zinthu zomwe iwo adazisiya pa dziko
lapansi ndi zomwe anali kuchita, zonsezi sizidawathandize.
83. Pamene Atumwi awo adadza kwa iwo ndi zizindikiro
zooneka, iwo adadzitama chifukwa cha nzeru zimene adali
nazo. Ndipo chimene anali kutsutsa chidagwa pa iwo.
84. Koma pamene iwo adaona chilango chathu, iwo adati,
"Ife takhulupirira mwa Mulungu mmodzi yekha ndipo
tili kuzikana zonse zimene tidali nazo zoonjezera pa Iye."
85. Koma chikhulupiriro chawo sichidawathandize china
chilichonse pamene adaona chilango chathu. Ili ndi lamulo
la Mulungu limene amaweruzira akapolo ake. Ndipo
pamenepo, anthu okana Mulungu adatayika kwambiri.

Sura 41 • Fussilat

# Fussilat

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. *Ha Mim.*

2. Chivumbulutso chochokera kwa Mulungu, Mwini
chifundo ndi Mwini chisoni chosatha. 3. Ndi Buku

limene mawu ake ndi ofotokozedwa mwatsatanetsatane.
Ndi Korani ya m'chiyankhulo cha Chiarabu, kwa anthu
ozindikira. 4. Lopereka nkhani yabwino ndi chenjezo
koma ambiri a iwo amabwerera m'mbuyo kotero sakumva
chilichonse. 5. Ndipo iwo amati, "Mitima yathu ndi
yokutidwa ku zimene iwe uli kutiitanira ndipo makutu
athu ndi ogontha ndipo chotchinga chili pakati pathu
ndi iwe kotero iwe gwira ntchito yako ndipo nafenso tili
kugwira yathu."

6. Nena, "Ine ndine munthu monga inu nomwe. Koma
zavumbulutsidwa kwa ine kuti Mulungu wanu ndi mmodzi
yekha kotero tsatirani njira yoyenera yopita kwa Iye ndipo
pemphani chikhululukiro chake. Tsoka kwa iwo amene
amafanizira milungu ina ndi Mulungu weniweni." 7. Iwo
ndi amene sapereka chaulere chothandiza osauka ndipo
sakhulupirira za m'moyo umene uli nkudza. 8. Ndithudi iwo
amene amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino,
kwa iwo kuli mphotho zosatha.

9. Nena, "Kodi, ndithudi, inu muli kumukana Iye
amene adalenga dziko lapansi m'masiku awiri ndipo muli
kumufanizira ndi ena kukhala ofanana naye? Iye ndi Ambuye
wa zolengedwa zonse." 10. Iye adaika mu dziko lapansi
mapiri okhazikika pamwamba pake ndipo adalidalitsa ilo
ndi kulipatsa chakudya, chokwanira chilichonse m'masiku
anayi ofanana. 11. Ndipo atatero Iye adabuka kumwamba
pamene kudali nkhungu ndipo Iye adati adayankhula
mawu okhudza kumwamba ndi ku dziko lapansi kuti,
"Idzani nonse mwanokha kapena mokakamizidwa." Onse
adati, "Tibwera mosakakamizidwa." 12. Ndipo Iye adakonza
ndi kulenga maiko asanu ndi awiri m'masiku awiri ndipo

adapereka ku dziko lililonse ulamuliro. Ndipo Ife tidaika
ku muyamba wapansi nyenyezi zokongola kuti zizilonda.
Umenewo ndi ulamuliro wa Mwini mphamvu ndi Mwini
nzeru.

13. Koma ngati iwo abwerera m'mbuyo, nena, "Ine
ndakuchenjezani inu za chilango chonga ngati chimene
chidadza pa anthu a Aad ndi Thamoud." 14. Ndipo pamene
Atumwi awo adadza kwa iwo kuchokera ku mbali zonse,
nati, "Musapembedze wina aliyense koma Mulungu." Iwo
adati, "Ngati Ambuye wathu akadafuna, Iye ndithudi,
akadatumiza Angelo. Kotero ife, ndithudi, sitikhulupirira
zimene inu mwatumidwa."

15. Akakhala anthu a Aad, iwo adanyada kopambana
padziko ndipo adati, "Kodi ali ndi mphamvu zopambana
zathu ndani?" Kodi iwo saona kuti Mulungu amene
adawalenga, ali ndi mphamvu zambiri zoposa zawo? Ndipo
iwo anali kukana chivumbulutso chathu. 16. Kotero Ife
tidawatumizira mphepo yamkuntho m'masiku a tsoka,
ndi cholinga choti alawe chilango chochititsa manyazi
m'dziko lino koma, ndithudi, chilango cha m'moyo
umene uli nkudza ndi chochititsa manyazi zedi ndipo iwo
sadzathandizidwa ayi. 17. Akakhala anthu a Thamoud Ife
tidawalangiza njira yoyenera koma iwo adasankha kuchita
zoipa m'malo mochita zabwino kotero kwa iwo kudadza
chilango chochititsa manyazi chifukwa cha ntchito zawo.
18. Ndipo Ife tidapulumutsa iwo amene adakhulupirira ndi
amene amaopa Mulungu ndi kulewa zoipa.

19. Ndipo pa tsiku limene adani ake a Mulungu
adzasonkhanitsidwa kupita kumoto, iwo adzaikidwa
m'magulumagulu. 20. Mpaka pamene wo atafika ku malo a

moto makutu awo, maso awo ndi makungu awo adzapereka
umboni wowaneneza pa zimene anali kuchita. 21. Ndipo
iwo adzati kwa makungu awo, “Bwanji inu muli kupereka
umboni wotineneza?” Iwo adzati, “Mulungu, amene
amayankhulitsa chilichonse, watiyankhulitsa ife ndipo
Iye ndiye amene adakulengani inu poyamba ndipo nonse
mudzabwerera kwa Iye.” 22. Ndipo inu simunadzibise ku
makutu anu, maso anu ndi makungu anu kuti zisadzapereke
umboni wokunenezani koma inu mumaganiza kuti
Mulungu sadziwa zonse zimene munali kuchita. 23. Ndipo
ndi maganizo anu amene inu munali kuganiza okhudza
Ambuye wanu amene wakubweretsani ku chionongeko
tsopano muli m’gulu la anthu otayika. 24. Ndipo ngati iwo
apirira komabe ku moto ndiko kudzakhala kumalo kwawo.
Ndipo ngati apempha chikhululukiro pempho lawo
lidzakanidwa.

25. Ndipo Ife tawasankhira anzawo amene adapanga
kuti aziona zopusa zakale ndi zatsopano kukhala zinthu
zokondweretsa kwa iwo. Ndipo chiweruzo chimene
chidadza ku mtundu wa majini ndi kwa anthu amene
adalipo kale chakwaniritsidwa kwa iwo. Ndithudi iwo ndi
otayika kwambiri.

26. Ndipo iwo amene sakhulupirira amati, “Musamvetsere
Koraniyi koma m’malo mwake muzipanga phokoso kuti
mwina mukhoza kuigonjetsa.” 27. Koma, ndithudi, Ife
tidzawalawitsa anthu osakhulupirira chilango chowawa,
ndipo, ndithudi, Ife tidzawalipira chifukwa cha ntchito
zawo zoipa zimene anali kuchita. 28. Amenewo ndiwo
malipiro a adani a Mulungu. Moto ndiwo malo awo a

nthawi zonse. Malipiro okwanira malinga ndi ntchito zawo
zoipa zimene anali kuchita pokana zizindikiro zathu.
29. Ndipo iwo osakhulupirira adzati, "Ambuye wathu!
Tilangizeni iwo amene ali pakati pa majini ndi anthu
amene adatisocheretsa ife ndipo ife tidzawapondaponda
ndi mapazi athu kuti iwo akhale a pansi kwambiri."
30. Ndithudi iwo amene amati, "Ambuye wathu ndi
Mulungu ndipo amapitiriza kutsatira njira yoyenera." Kwa
iwo angelo amadza nati, "Musaope ndipo musadandaule
ayi. Koma landirani nkhani yabwino yokhudza Paradiso
imene inu mudalonjezedwa!" 31. Ife tinali abwenzi anu
m'moyo uno ndiponso ndi m'moyo umene uli nkudza.
M'menemu inu mudzapeza chilichonse chimene mufuna
ndipo m'menemo inu mudzalandira chilichonse chimene
mupempha. 32. Mphatso yamtengo wapatali yachokera
kwa Iye amene amakhululukira nthawi zonse ndi Mwini
chisoni chosatha.
33. Kodi amayankhula bwino ndani kuposa iye amene
amati; 'Ambuye wanga ndi Mulungu' amaitanira anthu
kunjira ya Mulungu amene amachita ntchito zabwino
ndipo amati, "Ine ndine mmodzi wa Asilamu?" 34. Ntchito
zabwino ndi ntchito zoipa sizifanana. Kotero gonjetsani
choipa pochita chabwino ndipo, ndithudi, iye amene
ali mdani wako adzakhala ngati bwenzi lako lapamtima.
35. Koma palibe wina amene adzalandira zimenezi kupatula
yekhayo amene amapirira kwambiri ndipo amadziletsa.
Ndipo palibe wina amene angalandire kuposa iwo amene
ali ndi mwayi wochuluka. 36. Ndipo ngati iwe uyesedwa
ndi Satana, funafuna chitetezo cha Mulungu. Ndithudi

Iye ndiye amene amamva ndipo amadziwa chinthu china
chilichonse.
37. Ndipo pakati pa zizindikiro zake pali usiku ndi usana
ndiponso dzuwa ndi mwezi. Musagwadire dzuwa kapena
mwezi koma mugwadire Mulungu amene adazilenga izo
ngati ndiye amene inu mumamupembedza. 38. Koma
ngati iwo ndi amwano palibe kanthu chifukwa pamaso pa
Ambuye wako pali iwo amene amamulemekeza Iye usiku
ndi usana ndipo satopa ayi.
39. Ndipo pakati pa zizindikiro zake pali choti inu
mumaona nthaka ili youma koma pamene Ife titumiza pa
nthakayo madzi, iyo imakhala ndi moyo ndipo imakhala ndi
zomera zambiri. Ndithudi, Iye amapereka moyo ku nthaka
youma, ndithudi, akhoza kuperekanso moyo kwa anthu
amene adafa. Ndithudi Iye ali ndi mphamvu pa chinthu
china chilichonse. 40. Ndithudi onse amene sakhulupirira
chivumbulutso chathu sadzatha kubisala. Kodi iye amene
aponyedwa ku moto ndi wabwino kapena iye amene
adzapulumutsidwa pa tsiku lachiweruzo? Chitani monga
momwe mufunira. Ndithudi Iye amaona zonse zimene
mumachita.
41. Ndithudi iwo amene amakana uthenga pamene udza
kwa iwo adzalangidwa. Ndithudi ili ndi Buku lolemekezeka
kwambiri. 42. Bodza silingalowemo kuchokera kumbali ina
iliyonse. Ichi ndi chivumbulutso chochokera kwa Mwini
nzeru ndi olemekezeka. 43. Palibe chimene chili kunenedwa
kwa iwe kupatula chokhacho chimene chidanenedwa
kwa Atumwi kale. Ndithudi Ambuye wako ndi Mwini
kukhululukira ndiponso Mwini chilango chowawa.
44. Ndipo Ife tikadatumiza Buku la Korani mu chiyankhulo

china osati Chiarabu, iwo akadanena kuti, “Kodi bwanji
mawu ake sali kufotokozeredwa bwinobwino? Chiyani!
Chiyankhulo cha chilendo osati Chiarabu!” Nena, “Ilo
ndi la iwo amene amakhulupirira, ndi chilangizo ndiponso
mankhwala ochiritsa. Ndipo iwo amene sakhulupirira,
makutu awo ndi ogontha ndipo ilo ndi khungu kwa iwo.
Iwo ndiwo amene amaitanidwa kuchokera kutali.”
45. Ndithudi Ife tidamupatsa Mose Buku koma panabuka
mikangano yotsutsana za ilo. Koma pakanapanda
mawu amene adanenedwa kale ndi Ambuye wako, onse
akadaweruzidwa kale. Ndithudi iwo amakayika kwambiri.
46. Aliyense amene amachita zabwino amachitira moyo
wake zabwino ndipo aliyense amene amachita zoipa
amadzikundikira yekha mavuto. Ndithudi Ambuye wako
sapondereza akapolo ake.
47. Iye yekha ndiye amene amadziwa za ola. Ndipo palibe
mtengo umene umabereka zipatso kapena chachikazi
kuima kapena kubala popanda Iye kudziwa. Ndipo
pa tsiku limene adzawafunsa onse kuti, “Kodi ali kuti
amene munkati ndi anzanga?” Iwo adzayankha kuti, “Ife
tili kunenetsa kwa Inu kuti palibe aliyense pakati pathu
amene angachitire umboni.” 48. Ndipo mafano awo onse
adzawathawira ndipo onse adzadziwa kuti alibe kothawira
ayi.
49. Munthu satopa akamapempha zinthu zabwino koma
ngati mavuto adza pa iye, amataya mtima ndipo amakhala
ndi nkhawa. 50. Ndipo, ndithudi, Ife tikamuonetsera
chifundo chathu atazunzika, ndithudi iye adzati: “Ichi ndi
chifukwa cha nzeru zanga ndipo ine sindiganiza kuti ola
lidzadza. Ndipo ngati ine ndibwerera kwa Ambuye wanga,

nditħudi ine ndidzalandira zabwino kuchokera kwa Iye."
Ndithudi, Ife tidzawauza onse amene samakhulupirira
zonse zimene adachita ndipo, ndithudi, Ife tidzawapatsa
chilango chowawa kwambiri.
51. Ndipo Ife tikamulangiza munthu chifundo chathu,
iye amatembenuka ndi kuyamba kuchita zakezake koma
ngati vuto lidza pa iye, amapemphera mosalekeza. 52. Nena,
"Ndiuzeni ngati ilo ndi lochokera kwa Mulungu ndipo
inu muli kulikana. Kodi ndani amene angakhale wolakwa
kwambiri kuposa iye amene amatsutsa mowirikiza?"
53. Ife tidzawaonetsa zizindikiro zathu za mlengalenga ndi
za m'mizimu yawo, mpaka iwo atazindikira bwinobwino
kuti ndi choonadi chenicheni. Kodi sizikwanira kuti
Ambuye wanu ndiye mboni wa chinthu china chilichonse?
54. Ndithudi! Tsopano iwo ali okayika pa zakukumana ndi
Ambuye wawo. Ndithudi, ndiye amene wazungulira zinthu
zonse.

Sura 42 • Ash-Shûra

# Ash-Shura

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. *Ha Mim.* 2. *Ain Sin Qaf.*

3. Motero Mulungu, Mwini mphamvu ndi Mwini
nzeru amatumiza chivumbulutso kwa iwe monga anali
kuvumbulutsira kwa iwo amene adalipo iwe usanabadwe.
4. Iye ndiye Mwini wa chilichonse chimene chili

mlengalenga ndipo Iye ndi wapamwamba, ndiponso
wamkulu. 5. Kumwamba kumafuna kuphulika chifukwa
cha ulemerero wake ndipo angelo amaimba mayamiko
a Ambuye wawo ndipo amapempha chikhululukiro cha
zolengedwa zonse za padziko lapansi. Ndithudi, Mulungu,
ndiye amene amakhululukira ndipo ndi Mwini chisoni
chosatha. 6. Ndipo iwo amene amasankha ena ake kukhala
atetezi awo m'malo mwake, Mulungu amawayang'anira
ndipo iwe ulibe ulamuliro pa iwo.

7. Kotero tavumbulutsa kwa iwe Buku la Korani
m'Chiarabu, kuti ukhoza kuchenjeza make wa Mizinda
ndi iyo youzungulira. Ndipo kuti uchenjeze za tsiku la
chiweruzo limene mosakayika lidzadza pamene gulu lina
lidzakhala ku Paradiso ndi gulu linzake lidzakhala kumoto.
8. Ndipo ngati Mulungu akadafuna, akadawapanga
onse kukhala mtundu umodzi koma Iye amasankha
amene wamufuna kulandira chisomo chake ndipo onse
osalungama sadzapeza mtetezi kapena wowathandiza.
9. Kodi kapena iwo asankha kuti aziwapembedza atetezi
ena m'malo mwake? Koma Mulungu ndiye Mtetezi. Ndipo
ndiye amene amapereka moyo kwa akufa ndipo Iye ali
ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse. 10. Ndipo pa
chilichonse chimene mumatsutsana, chiweruzo chake chili
ndi Mulungu Mwini wake. Ameneyo ndi Mulungu weniweni,
Ambuye wanga ndipo mwa Iye ine ndimakhulupirira ndipo
kwa Iye ndiko ndimalapa machimo anga.

11. Namalenga wakumwamba ndi dziko lapansi. Iye
adalenga anzanu kuchokera pakati panu ndi anzawo
kuchokera ku nyama. Mwanjira imeneyi Iye amakulengani
inu. Palibe chilichonse chofanana naye ndipo Iye ndi

wakumva ndi woona. 12. Iye ndiye amene ali ndi makiyi
a kumwamba ndi a pa dziko lapansi. Iye amachulukitsa
kapena kuchepetsa chakudya cha aliyense amene
wamufuna. Ndithudi Iye amadziwa bwino za chinthu
china chilichonse.
13. Iye wakukhazikitsirani chipembedzo chimene
adakhazikitsira Nowa kuti atsatire, ndi chimene
tavumbulutsa kwa iwe, ndi chimene tidakhazikitsira
Abrahamu ndi Mose ndi Yesu powauza kuti inu
mukhazikitse chipembedzo ndipo musapatukane. Ndi
kovuta kuti anthu osakhulupirira atsatire zimene iwe
uwaitanira. Mulungu amasankha yekha onse amene
wawafuna ndipo amatsogolera onse amene amagonja kwa
Iye.
14. Koma iwo adapatukana pamene nzeru zidadza kwa
iwo ndipo anali kuchitirana mwano. Koma kukadakhala
kuti padalibe mawu amene adanenedwa kale kuchokera
kwa Ambuye wako wokhudza chimaliziro, chiweruzo
chikadadza kale pa iwo. Ndipo, ndithudi, iwo amene
adalandira Buku pambuyo pawo, ndithudi, ali ndi chikayiko
chachikulu pa icho.
15. Kotero pitiriza kuwaitana ndipo limbikira potsatira
njira yoyenera monga momwe walamulidwira. Iwe
usatsatire zilakolako zawo zachabe, ndipo nena, “Ine
ndimakhulupirira mawu onse a Mulungu amene
wavumbulutsa mu Buku lake, ndipo ine ndalamulidwa
kuonetsa chilungamo pakati panu. Mulungu ndi Ambuye
wathu ndiponso Ambuye wanu. Kwa ife ntchito zathu
ndipo kwa inu ntchito. Ndipo palibe mkangano pakati
pa ife ndi inu. Mulungu adzatisonkhanitsa tonse ndipo

ndi kwa Iye kumene tonse tidzabwerera.” 16. Ndipo iwo
amene amatsutsa za Mulungu atavomereza kale kuti
adzamumvera, mitsutso yawo siidzakhala yomveka kwa
Ambuye wawo ndipo mkwiyo wake udzadza pa iwo ndipo
iwo adzalangidwa kwambiri!
17. Ndi Mulungu amene watumiza Buku mwachoonadi ndi
muyeso. Kodi ndi chiyani chimene chingakudziwitseni inu
kuti mwina ola lachiweruzo lili pafupi? 18. Okhawo amene
sakhulupilira amafuna kuti ola lidze msanga pamene onse
amene amakhulupirira amaliopa ilo chifukwa amadziwa
kuti ndi loonadi. Ndithudi onse amene amakana za olali
ndi otayika kwambiri.
19. Mulungu ndi wachifundo ndi wachisoni kwa akapolo
ake. Iye amapereka chakudya kwa aliyense amene
wamufuna. Ndipo Iye ndi wamphamvu ndi Mwini
mphamvu zonse. 20. Aliyense amene afuna zabwino za
m’moyo umene uli nkudza, Ife tidzamupatsa zambiri
ndipo wina aliyense amene afuna zabwino za m’moyo uno
tidzamupatsa koma iye sadzakhala ndi gawo lina m’moyo
umene uli nkudza.
21. Kodi kapena iwo ali ndi anzawo amene akhazikitsa
chipembedzo china popanda chilolezo cha Mulungu?
Ndipo pakadapanda kuti mawu adanenedwa kale,
chiweruzo chikadafika kale pakati pawo. Ndithudi anthu
ochita zoipa adzalandira chilango chowawa kwambiri.
22. Iwe udzawaona anthu ochimwa ali ndi mantha chifukwa
cha ntchito zawo ndipo ndithudi mazunzo adzadza pa
iwo pamene iwo amene amakhulupirira ndipo amachita
ntchito zabwino, adzakhala ku Paradiso. Iwo adzalandira,
kuchokera kwa Ambuye wawo zonse zimene adzafuna.

Chimenechi ndicho chisomo chachikulu. 23. Imeneyi ndi
nkhani yabwino imene Mulungu ali kuwauza akapolo ake
amene amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino.
Nena, “Ine sindili kukupemphani malipiro ayi kupatula
kuti muzionetsa chikondi kwa ine chifukwa cha ubale
wanga ndi inu.” Ndipo aliyense amene alandira chabwino,
tidzamuonjezera zabwino zambiri mofanana ndi izo.
Ndithudi Mulungu ndi wokhululukira ndi wokonzeka
kulipira.
24. Kapena iwo akuti, “Iye wapeka yekha bodza lokhudza
Mulungu?” Ngati Mulungu akadafuna akadatseka
mtima wako. Ndipo Mulungu amafafaniza bodza ndi
kukhazikitsa choonadi ndi mawu ake. Ndithudi Iye
amadziwa zinsinsi zonse zimene zili m’mtima. 25. Ndiye
amene amavomera kulapa kwa akapolo ake ndipo Iye
amawakhululukira machimo awo ndipo Iye amadziwa
zonse zimene mumachita. 26. Ndipo Iye amayankha onse
amene amakukhulupirira ndi kuchita ntchito zabwino
ndipo amawapatsa zambiri kuchokera ku chisomo chake.
Akakhala anthu osakhulupirira iwo adzalandira chilango
chowawa.
27. Ndipo ngati Mulungu akadaonjezera zabwino kwa
akapolo ake, ndithudi, iwo akadaswa malamulo mopyola
muyeso pa dziko lonse. Koma Iye amatumiza atayesa
mwachifuniro chake. Ndithudi Iye amalemekeza akapolo
ake, amadziwa zonse ndipo amayang’anitsitsa akapolo ake.
28. Ndipo ndiye amene amagwetsa mvula pa nthawi imene
iwo ataya chikhulupiriro ndipo amaonetsa chifundo chake
ponseponse. Ndipo Iye ndiye Mtetezi wamphamvu ndi
Woyenera kulemekezeka. 29. Ndipo pakati pa zizindikiro

zake, pali kalengedwe ka kumwamba ndi dziko lapansi ndi
zolengedwa zamoyo zimene adazimwaza monsemu. Ndipo
Iye ali ndi mphamvu yozisonkhanitsa zonse pamodzi
pamene Iye wafuna.
30. Ndipo mavuto onse amene amagwa pa inu
amadza chifukwa cha ntchito zanu. Komabe Iye
amakukhululukirani zolakwa zanu zambiri. 31. Ndipo inu
simungathe kuthawa padziko lapansi ndipo inu mulibe
wina aliyense kupatula Mulungu amene angakutetezeni
kapena kukuthandizani.
32. Ndipo pakati pa zizindikiro zake pali zombo zonga
mapiri zimene zimayenda pa nyanja. 33. Ngati Iye afuna, Iye
amaimitsa mphepo ndipo iwo amaima osayenda pamwamba
pa nyanja. Ndithudi mu zimenezi muli zizindikiro kwa
aliyense amene amapirira ndipo amayamika. 34. Kapena
akhoza kuwaononga chifukwa cha zolakwa zimene iwo
adachita. Koma Iye amawakhululukira zolakwa zambiri.
35. Onse amene amakana chivumbulutso chathu ayenera
kudziwa kuti alibe malo othawirako.
36. Motero chilichonse chimene mwapatsidwa padziko
lapansi ndi chongosangalatsa cha m'moyo uno koma chimene
chili ndi Mulungu ndi chabwino ndiponso chosatha kwa iwo
amene amakhulupirira ndipo amaika chikhulupiriro chawo
mwa Ambuye wawo. 37. Ndi iwo amene amapewa kuchita
machimo aakuluakulu ndi zinthu zochititsa manyazi ndipo
pamene akwiya amakhululuka. 38. Iwo amene amamvera
kuitana kwa Ambuye wawo ndipo amapemphera panthawi
yake amachita zinthu zawo atakambirana ndiponso
amapereka kuchokera ku zinthu zimene tawapatsa iwo.
39. Ndi iwo amene akaponderezedwa, amabwezera. 40. Ndipo

kubwezera kwa ntchito zoipa ndi choipa cholingana ndi ntchitozo ngati munthu akhululukira mnzake ndi kusintha maganizo ake, iye adzalandira mphotho yake kuchokera kwa Mulungu. Ndithudi Iye sakonda anthu osalungama.
41. Ndipo aliyense amene amabwezera ataponderezedwa, iye sadzakhala ndi mlandu wina uliwonse. 42. Mlandu uli pa iwo amene amapondereza anthu pochita zoipa ndipo mwamwano amaswa malamulo mopyola muyeso padziko. Ndipo kwa otere kudzakhala chilango chowawa kwambiri.
43. Ndipo, ndithudi, aliyense amene aonetsa kupirira ndi chikhululukiro, chimenechi ndi chimodzi cha zinthu zimene zimayamikidwa ndi Mulungu.

44. Kwa aliyense amene Mulungu amusocheretsa, kulibe wina amene angamuteteze. Ndipo iwe udzawaona anthu ochita zoipa pamene iwo adzaona chilango ali kunena kuti, "Kodi pali njira yoti tingathe kubwerera?" 45. Ndipo iwe udzawaona ali kubweretsedwa kuchilango monyozedwa ndipo ali ndi nkhope zachisoni. Ndipo iwo amene amakhulupirira adzati, "Ndithudi otayika ndi anthu amene adzitaya ndi owatsatira awo patsiku lachiweruzo. Ndithudi anthu ochita zoipa adzakhala ku chilango chosatha."
46. Ndipo iwo sadzakhala ndi abwenzi oti awathandize kupatula Mulungu. Ndipo aliyense amene Mulungu wamusocheza alibe wina womutsogolera.

47. Kotero bwererani kwa Ambuye wanu mwamsanga tsiku limene simungathe kubwerera lisanadze. Inu simudzakhala ndi kothawira pa tsiku limeneli ndipo inu simudzakhala ndi mwayi wokana. 48. Koma ngati iwo akana, Ife sitidakutumize iwe ngati owayang'anira iwo. Udindo wako ndi kungopereka uthenga. Ndipo, ndithudi,

ngati Ife timupanga munthu kulawa chisomo chathu, iye
amasangalala kwambiri chifukwa cha chisomocho koma
ngati vuto lidza pa iwo chifukwa cha zolakwa zawo zimene
adachita, ndithudi munthu amakhala osayamika.

49. Ufumu wa kumwamba ndi wa dziko lapansi Mwini
wake ndi Mulungu. Ndipo Iye amalenga chimene wafuna.
Iye amapereka ana aakazi kwa amene Iye wamufuna ndipo
amapereka ana aamuna kwa amene wamufuna. 50. Kapena
amawapatsa, ana aamuna ndi ana aakazi, ndipo amapanga
amene wamufuna kuti akhale chumba. Ndithudi iye
amadziwa zonse ndipo amatha kuchita chilichonse.

51. Si koyenera kuti Mulungu ayankhule ndi munthu
kupatula kudzera m'chivumbulutso kapena kuchokera
kumalo obisika kapena potumiza Mtumwi kudzawauza,
chimene Mulungu afuna ndi chilolezo chake. Ndithudi
Iye ndi wapamwamba ndi wanzeru zosatha. 52. Kotero,
mwaulamuliro wathu, tatumiza chivumbulutso chathu
kwa iwe. Iwe siumadziwa kuti chivumbulutso chidali
chiyani kapena kuti chikhulupiriro chidali chiyani. Koma
Ife tachipanga icho kukhala muuni umene timatsogolera
nawo akapolo athu mwachifuniro chathu. Ndithudi iwe
umalangiza anthu ku njira yoyenera. 53. Njira ya Mulungu
amene ali Mwini wake wa chilichonse chimene chili
mlengalenga ndi chilichonse chimene chili pa dziko lapansi.
Ndithudi kwa Mulungu zinthu zonse zimabwerera.

# ZUKHRUF

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. *Ha mim.*

2. Ndilumbira pali Buku limene limafotokoza zinthu
mosabisa. 3. Ndithudi talipanga ilo kukhala Korani
yam'chinenero cha Chiarabu kuti iwe ukhoza kulizindikira.
4. Ndithudi ilo lili mu Make Buku limene lili pamaso pathu,
lolemekezeka ndi lodzala ndi nzeru.

5. Kodi Ife tisiye kukukumbutsani inu nonse chifukwa
chakuti ndinu anthu osasamala ndi oswa malamulo? 6. Kodi
ndi Atumwi angati amene Ife tidatumiza ku mitundu ya
anthu akale? 7. Ndipo kwa iwo sikunadze Mtumwi amene
iwo sadamunyoze. 8. Kotero Ife tidawaononga, anthu
amphamvu kuposa awa, ndipo chitsanzo cha anthu onse
akale chadutsa.

9. Ndithudi ngati iwe ukawafunsa kuti, "Kodi ndani
adalenga kumwamba ndi dziko lapansi?" Iwo, ndithudi,
adzakuyankha kuti, "Mwini mphamvu ndi Mwini wodziwa
ndiye amene adazilenga." 10. Iye ndi amene adalenga dziko
kukhala malo anu a mpumulo ndipo adaika mu ilo njira kuti
inu mukhoza kutsogozedwa bwino. 11. Ndipo ndiye amene
amatumiza mvula kuchokera kumitambo molingana ndi
muyeso. Ndipo Ife timadzutsa nthaka imene idali yakufa
ndi iyo, kotero nanunso mudzadzutsidwa chimodzimodzi.
12. Ndipo ndiye amene adalenga zinthu ziwiriziwiri

ndipo adapanga zombo ndi nyama kuti muzikwera.
13. Kuti inu mukhoza kukhala okhazikika pa misana pawo
ndi kukumbukira ubwino wa Ambuye wanu pamene
mumakhazikikapo ndi kunena kuti, "Ulemerero ukhale
kwa Iye amene adazipanga izo kukhala zopanda mphamvu
kwa ife ndipo ife sitikadatha kutero." 14. "Ndithudi kwa
Ambuye wathu ife tidzabwerera."
15. Komabe iwo amawapatsa ena mwa akapolo ake gawo
lake. Ndithudi munthu ndi wosayamika. 16. Kodi Iye
wadzisankhira ana aakazi kuchokera ku zimene walenga
ndipo adakusankhani inu kukhala ndi ana aamuna?
17. Ndipo ngati wina wa iwo auzidwa nkhani za chimene
Iye amati ndi chofanana ndi Mulungu, nkhope yake
imada ndipo amakhala wokwiya. 18. Icho ndi chimene
chidapangidwa ngati chosangalatsa ndipo pa mtsutso,
icho sichingathe kuyankhula bwinobwino. 19. Ndipo iwo
amasandutsa angelo amene ali akapolo a Mulungu, kukhala
akazi. Kodi iwo adaonerera chilengedwe chawo? Umboni
wawo udzalembedwa ndipo iwo adzafunsidwa!
20. Ndipo iwo adati, "Chikadakhala chifuniro cha Mwini
Chisoni Chosatha, ife sitikadapembedza milungu ina." Iwo
sadziwa china chilichonse chokhudza chimenechi. Ndipo
iwo amangonama chabe. 21. Kodi kapena Ife tidawapatsa
Buku lina ili lisanadze limene iwo ali kukhulupilira?
22. Iyayi! Iwo amati, "Ife tidapeza makolo athu ali
kutsatira njira ina ndi chipembedzo china chake ndipo ife
timatsogozedwa potsatira zimene iwo amachita." 23. Ndipo
Ife sitidatumize Mchenjezi iwe usanadze kwa anthu ena,
koma achuma amene anali kukhala pakati pawo ankati;
"Ife tidapeza makolo athu ali kutsatira njira yina ndi

chipembedzo china chake ndipo ndithudi ife tidzatsatira
zimene iwo anali kuchita.” 24. Iye adati; “Ngakhale kuti ine
nditakubweretserani langizo labwino loposa limene mukuti
mudapeza makolo anu ali kutsatira?” Iwo adati, “Ndithudi
ife sitikhulupirira zimene iwe ukuti watumizidwa.”
25. Kotero Ife tidagwetsa chilango pa iwo ndipo taona
mmene chinalili chimaliziro cha iwo amene adakana
choonadi.

26. Ndipo Abrahamu adawauza abambo ake pamodzi
ndi anthu ake kuti, “Ndithudi ine ndili kudzipatula ku
zimene inu mupembedza.” 27. “Kupatula yekhayo amene
adandilenga ine ndipo, ndithudi, Iye adzanditsogolera.”
28. Ndipo adawapanga mawu kuti akhazikike mwa iwo
amene adadza iye atachoka kuti akhoza kubwerera.
29. Iyayi! Koma Ine ndidawapatsa ,iwo ndiponso makolo
awo, chisangalalo mpaka pamene choonadi chidadza
kwa iwo ndi Mtumwi amene anali kuwafotokozera zonse
momveka. 30. Koma pamene choonadi chidadza pa iwo,
iwo adati, “Awa ndi matsenga ndipo ife sitikhulupirira mwa
iwo.”

31. Ndipo iwo amati: “Bwanji Korani iyi siidatumizidwe
kwa munthu wina wotchuka wochokera ku Mzinda wina
pakati pa Mizinda iwiri?” 32. Kodi ndiwo amene akhoza
kugawa gawo lina la chisomo cha Ambuye wako? Ndife
amene timagawa pakati pawo chakudya chawo cha moyo
uno ndipo tawakweza ena kukhala apamwamba kuposa
anzawo kotero kuti akhoza kulemba ntchito anzawo. Koma
chisoni cha Ambuye wako ndi chabwino kwambiri kuposa
chuma chimene amasonkhanitsa. 33. Ndipo zikadakhala
kuti anthu onse anali a chipembedzo chimodzi, ndithudi,

Ife tikadawapatsa onse amene sakhulupirira mwa
Mulungu madenga a siliva kuti aike pa nyumba zawo ndi
pa makwerero oti azikwererapo. 34. Ndipo nyumba, zitseko
ndi mipando, zonse zikadakhala za siliva kuti azikhalapo.
35. Ndipo zipangizo zina zikadakhala za golide. Komabe
zonsezi sizikadakhala chinthu china koma chisangalalo cha
m'moyo uno. Ndipo moyo umene uli nkudza, umene uli
ndi Ambuye wako, ndi wa anthu ochita ntchito zabwino.

36. Aliyense amene asiya kukumbukira Mwini chisoni
chosatha, Ife timamusankhira iye Satana kuti akhale
bwenzi lake la pamtima. 37. Ndipo, ndithudi, iwo
amangowasokoneza ku njira yoyenera koma iwo amaganiza
kuti ali kutsogozedwa bwino. 38. Mpaka pamene wotereyu
abwerera kwa Ife, iye amati, pomuuza bwenzi lake la
pamtima, "Kukadakhala kuti pakati pa ine ndi iwe panali
mtunda wotalika monga kutalikirana kwa kum'mawa
kuwiri!" Bwenzi loipa lenileni! 39. Ndipo popeza inu munali
kuchita zoipa, lero sizidzakuthandizani popeza nonse
ndinu olandira chilango.

40. Kodi iwe ungawapange agonthi kumva kapena
kutsogolera anthu akhungu kapena kutsogolera iye amene
ndi ochimwa? 41. Ndipo Ife tikakutenga, Ife, ndithudi,
tidzagwetsa chilango chathu pa iwo. 42. Kapena ngati Ife
titakuonetsa zina zimene tawalonjeza iwo, ndipo ndithudi,
Ife tili ndi mphamvu pa zinthu zonse. 43. Kotero gwiritsa
chimene chavumbulutsidwa kwa iwe. Ndithudi iwe uli pa
njira yoyenera. 44. Ndipo ndithudi Ichi ndi chikumbutso
kwa iwe ndi kwa anthu ako ndipo posachedwapa
mudzafunsidwa. 45. Ndipo afunse iwo za Atumwi athu
amene Ife tidawatuma iwe usanabadwe. Kodi Ife

tidasankha milungu ina yoti izipembedzedwa yoonjezera
pa Mwini Chisoni Chosatha?
46. Ndipo, ndithudi, Ife tidamutumiza Mose ndi uthenga
wathu kwa Farawo ndi mafumu ake ndipo iye adati,
"Ndithudi ine ndine Mtumwi wa Ambuye wa zolengedwa
zonse." 47. Koma pamene iye adadza kwa iwo ndi
zizindikiro zathu zooneka, iwo adaziseka zizindikirozo.
48. Tidawaonetsa zizindikiro zosiyanasiyana, chilichonse
chopambana chinzake, ndipo Ife tidawapatsa chilango
kuti akhoza kutembenuka. 49. Ndipo iwo adati, "Oh iwe
munthu wamatsenga! Mupemphe Ambuye wako m'malo
mwathu, molingana ndi lonjezo limene Iye adapanga ndi
iwe. Ndithudi ife tidzatsatira njira yoyenera." 50. Koma
pamene tidawachotsera chilango, iwo adaphwanya lonjezo
lawo.
51. Ndipo Farawo adalengeza pamaso pa anthu ake kuti,
"Oh inu anthu anga! Kodi Ufumu wa dziko la Aiguputo si
wanga? Nanga mitsinje imene ilikuyenda pansi pa mapazi
anga, kodi simuli kuiona?" 52. "Kodi ine sindine wopambana
kwambiri kuposa munthu wonyozeka amene ali kukanika
kuyankhula momveka?" 53. "Nanga ndi chifukwa chiyani
iye sadavekedwe zigwinjiri za golide kapena bwanji
silinadze ndi iye gulu la angelo lomuperekeza?" 54. Motero
iye adawapusitsa anthu ake ndipo iwo amamumvera iye.
Ndithudi iwo adali anthu onyoza. 55. Ndipo pamene iwo
adatikwiyitsa, Ife tidawagwetsera chilango ndipo onse
tidawamiza m'madzi. 56. Ndipo tidawapanga iwo kukhala
phunziro kwa mibadwo yam'tsogolo.
57. Ndipo pamene mwana wamwamuna wa Maria
atchulidwa ngati chitsanzo, taona! Anthu ako amaseka.

58. Ndipo iwo amati, “Kodi milungu yathu ndiyo yopambana
kapena iyeyo ndiye wopambana?” Izi amangozinena kwa
iwe ndi cholinga chofuna mikangano ndipo iwo ndi anthu
amwano. 59. Iye sadali wina koma kapolo wathu amene
tidamulangiza chisomo chathu, ndipo tidamupanga Iye
kukhala chitsanzo kwa ana a Israyeli. 60. Ndipo tikadafuna
tikadapanga ena a inu kukhala angelo kuti akhale padziko
m'malo mwanu. 61. Ndithudi ichi ndi chizindikiro cha
ola, kotero musakayike za ilo ndipo nditsateni ine. Iyo
ndiyo njira yoyenera. 62. Ndipo musalole kuti Satana
akutchinjirizeni chifukwa, ndithudi, iye ndi mdani wanu
weniweni.

63. Pamene Yesu adadza ndi zizindikiro zooneka
adati, “Tsopano ndadza kwa inu ndi luntha ndi cholinga
chokuuzani tsatanetsatane za fundo zina zimene
mumatsutsana. Motero opani Mulungu ndipo mundimvere
ine.” 64. “Ndithudi Mulungu! Ndiye Ambuye wanga ndi
Ambuye wanu. Motero mutumikireni Iye. Imeneyi ndiyo
njira yoyenera.” 65. Koma magulu ena a pakati pawo
adapatukana, kotero tsoka kwa iwo amene adali oipa
chifukwa cha chilango chowawa chimene chidzadza pa iwo
patsiku la masautso.

66. Kodi iwo ali kungodikira kuti ola lidzadza pa iwo
mwadzidzidzi pamene iwo sali kudziwa? 67. Abwenzi
patsiku limeneli adzasanduka adani kupatula okhawo
amene amalewa zoipa. 68. Oh inu akapolo anga! Palibe
chochititsa mantha kwa inu lero lino ndipo simudzamva
chisoni. 69. Inu amene mwakhulupirira chivumbulutso
chathu ndipo munali Asilamu. 70. Lowani m'Paradiso,
inu pamodzi ndi akazi anu ndipo mudzasangalatsidwa.

71. Mbale za golide ndi zikho zomwera zidzaperekedwa
kwa iwo ndipo mu izo mudzakhala zimene mitima yawo
inali kulakalaka ndi ponso zosangalala kuziona. Ndipo inu
mudzakhala momwemo mpaka kalekale. 72. Ndipo uwu ndi
munda umene mwapatsidwa kuti mukhalemo chifukwa
cha zimene mudachita. 73. M'menemo mudzapeza zipatso
zochuluka zimene muzidzadya.
74. Ndithudi onse osakhulupirira adzakhala ku moto
wa ku Gahena mpaka kalekale. 75. Chilango chawo
sichidzachepetsedwa ndipo adzasowa chonena chifukwa
adzakhala ndi mantha. 76. Ife sitidawalakwire koma iwo
adadzilakwitsa okha. 77. Ndipo iwo adzalira kuti, "Oh
Maliki! Muuze Ambuye wako kuti atimalize ife! Ndipo
iye adzati, "Ndithudi inu mudzakhalabe ndi moyo."
78. Ndithudi Ife tabweretsa choonadi kwa iwe koma
ambiri a inu mumadana ndi choonadi. 79. Kapene iwo ali
ndi chikonzekero china? Motero nafenso tili kukonzeka.
80. Kapena iwo amaganiza kuti Ife sitikumva zimene
amabisa ndi nkhani zawo za chinsinsi? Ndithudi Ife
timamva ndipo Atumwi athu amene ali pakati pawo
amalemba chilichonse.
81. Nena, "Ngati Mwini Chisoni Chosatha akadakhala
ndi Mwana, ine ndikadakhala woyamba kumupembedza."
82. "Ulemerero ukhale kwa Ambuye wakumwamba ndi
dziko lapansi, Ambuye Mwini mpando wachifumu!
Iye akhale pamwamba pa zimene amukundukira Iye."
83. Kotero aleke kuti ayambe kuyankhula zinthu zopanda
pake ndi kusewera mpaka pamene akumana ndi tsiku
limene amaopsedwa nalo.
84. Iye ndiye Mulungu wakumwamba ndi Mulungu wa

padziko lapansi ndipo Iye ndi waluntha ndi wodziwa
chinthu china chilichonse. 85. Ndipo wodala ndi Mwini
Ufumu wakumwamba ndi dziko lapansi ndi zonse zimene
zili m’menemo. Iye ndiye amene amadziwa ola lachiweruzo
ndipo kwa Iye ndi kumene nonse mudzabwerera.
86. Ndipo onse amene amawapembedza oonjezera
pa Mulungu alibe mphamvu yowaimirira kupatula
yekhayo amene amachitira umboni woona ndiye amene
iwo amamudziwa. 87. Ndipo ngati iwe utawafunsa kuti
kodi adawalenga ndani? Ndithudi iwo adzayankha kuti,
“Mulungu.” Nanga ndi chifukwa chiyani amasiya choonadi?
88. Ndi zonena zake kuti, “Ambuye wanga! Ndithudi awa
ndi anthu amene safuna kukhulupirira.” 89. Kotero asiye
okha ndipo nena, “Mtendere!” Koma iwo adzadziwa
posachedwapa.

Sura 44 • Ad-Durhân

# Ad-Dukhan

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. *Ha Mim!*

2. Ndilumbira pali Buku limene limanena zoona. 3. Ife
tidalivumbulutsa ilo mu usiku wodalitsika. Ndithudi Ife
tili kupitirizabe kuchenjeza. 4. Mu umenewu, ntchito
iliyonse ili kuonetsedwa poyera. 5. Lamulo lochokera kwa
Ife, ndithudi Ife timatumiza. 6. Chifundo chochokera kwa
Ambuye wako, ndithudi Iye ndi wakumva ndi wodziwa.

7. Ambuye wakumwamba ndi dziko lapansi ndi zonse
zimene zili pakati pawo, ngati inu nonse mutakhala ndi
chikhulupiriro chenicheni. 8. Kulibe Mulungu wina koma
Iye yekha. Ndipo ndiye amene amapereka moyo ndi
imfa. Ambuye wako ndi Ambuye wa makolo ako amene
adanka kale. 9. Iyayi! Iwo amakayika, amasewerera.
10. Motero dikirani tsiku limene kumwamba kudzatsitsa
utsi wooneka. 11. Umene udzazungulira anthu ndipo
chimenechi ndi chilango chowawa. 12. Iwo adzati, "Ambuye
wathu! Tichotsereni chilango ichi chifukwa tsopano
takhulupirira." 13. Kodi iwo angachenjezedwe bwanji
pamene kunadza kale Mtumwi amene anali kuwauza
choonadi? 14. Iwo adamutembenukira ndi kumati, "Munthu
wophunzitsidwa ndi anthu ena, munthu wamisala."
15. Ndithudi Ife tidzachotsa chilango pa kanthawi kochepa
koma ndithudi inu mudzabwerera. 16. Patsiku limene Ife
tidzakugwirani mwamphamvu. Ndithudi tidzawabwezera
chilango choyenera.

17. Ndipo, ndithudi, tidawayesa anthu a Farawo,
iwo asanabadwe, ndipo kudadza kwa iwo Mtumwi
wolemekezeka. 18. Naati "Bweretsani kwa ine akapolo a
Mulungu." "Ndithudi ine ndine Mtumwi wokhulupirika
kwa inu." 19. "Ndipo musachitire mwano Mulungu.
Ndithudi ine ndadza kwa inu ndi ulamuliro wooneka."
20. "Ndipo ndithudi ine ndapempha chitetezo cha Ambuye
wanga ndi Ambuye wanu kuti musandiononge." 21. "Koma
ngati inu simundikhulupirira ine, ndiye mundisiye ndekha."

22. Ndipo iye anati kwa Ambuye wake, "Anthu awa
ndi ochimwa." 23. Choka iwe ndi akapolo anga nthawi
yausiku. Ndithudi iwe udzalondoledwa. 24. "Ileke nyanja

kukhala monga mmene ili. Ndithudi iwo ndi anthu amene
adzamizidwa.” 25. Kodi ndi minda ingati ndiponso a kasupe
angati amene iwo adasiya? 26. Ndi minda ya chimanga
ndi malo olemekezeka! 27. Ndi zinthu zabwino zimene
amasangalala nazo. 28. Kotero zinali choncho. Ndipo
Ife tidawasankha anthu ena kuti atenge zinthu zawo.
29. Kumwamba kapena dziko lapansi silidakhetse msozi
chifukwa cha iwo ndipo iwo sadapatsidwe mpumulo.
30. Ndithudi tidapulumutsa ana a Israyeli ku chilango
chochititsa manyazi. 31. Chimene chidaperekedwa ndi
Farawo. Ndithudi iye adali wamwano ndi mmodzi wa
anthu oswa malamulo. 32. Ndithudi tidawasankha iwo kuti
akhale ndi nzeru kuposa mitundu ina. 33. Ndipo tidawapatsa
chivumbulutso chimene chidali ndi mayesero ooneka.
34. Ndithudi iwo akuti, 35. “Palibe china chilichonse
kupatula imfa yathu yoyamba ndipo ife sitidzaukitsidwa
kwa akufa.” 36. “Kotero bweretsa makolo athu ngati
zimene ukunena ndi zoona!” 37. Kodi awa ndi opambana
kuposa anthu a Tubba ndi iwo amene adalipo kale? Ife
tidawaononga onse ndipo iwo adali olakwa.
38. Ndipo ife sitidalenge kumwamba ndi dziko lapansi
ndi zonse zimene zili m’menemo mwamasewera. 39. Ife
sitidazilenge zonsezi kupatula mwachoonadi ndipo
ambiri a iwo sadziwa. 40. Ndithudi tsiku lachimaliziro
ndi tsiku lomaliza kwa iwo onse. 41. Ndi tsiku limene
bwenzi sadzakumbukira bwenzi ake ndipo sadzalandira
chithandizo. 42. Kupatula yekhawo amene waonetsedwa
chisomo cha Mulungu. Ndithudi Iye ndiye Mwini
mphamvu ndi Mwini chisoni chosatha.
43. Ndithudi mtengo wa Zaqqum. 44. Udzakhala chakudya

cha anthu ochimwa. 45. Monga mafuta owira, chidzabwata
m'mimba mwawo. 46. Monga ngati madzi ogaduka.
47. "Mugwire iye ndipo mududuzireni m'kati mwa Gahena."
48. Ndipo thirani pamutu pake chilango cha madzi owira.
49. "Lawani ichi! Ndithudi inu munali amphamvu ndi
aulemu." 50. "Ndithudi! Ichi ndicho chimene munali
kukayika."

51. "Ndithudi! Iwo amene amalewa zoipa adzakhala
kumalo otetezedwa." 52. Pakati pa minda ndi a kasupe.
53. Iwo atavala Silika wokhuthala ndi wokongola, atakhala
moyang'anizana. 54. Kotero zidzakhala choncho ndipo Ife
tidzawakwatitsa kwa akazi a maso aakuluakulu okongola.
55. Iwo adzaitanitsa chipatso cha mtundu uliwonse
mwamtendere ndi mokhazikika. 56. Ndipo iwo sadzalawa
imfa kupatula imfa yoyamba ndipo Iye adzawapulumutsa
ku chilango chowawa cha Gahena. 57. Chisomo chochokera
kwa Ambuye wako! Chimenechi chidzakhala chinthu
chopambana kwambiri.

58. Ndithudi Ife taipanga Koraniyi kukhala yapafupi
m'chiyankhulo chako ndi cholinga chakuti mwina angathe
kukumbukira. 59. Kotero iwe dikira chifukwa nawonso ali
kudikira.

# Al Jasiyah

M'dzina la Mulungu, Mwini chifundo ndi Mwini
chisoni chosatha.

1. *Ha Mim.*

2. Chivumbulutso cha Buku ndi chochokera kwa Mulungu,
Mwini mphamvu zonse ndi Mwini nzeru. 3. Ndithudi
kumwamba ndi dziko lapansi kuli zizindikiro kwa anthu
okhulupirira. 4. M'chilengedwe chanu nyama zimapezeka
paliponse pa dziko lapansi ndipo ndi zizindikiro kwa iwo
amene ali okhulupirira kwenikweni. 5. Ndi m'kasinthidwe
ka usiku ndi usana ndi m'chakudya chimene amatumiza
kuchokera ku mitambo ndipo amapereka moyo ku nthaka
imene idali yakufa ndipo m'kasinthidwe ka mphepo, muli
zizindikiro kwa anthu ozindikira. 6. Ichi ndi chivumbulutso
chochokera kwa Mulungu chimene tili kulakatula kwa
iwe mwachoonadi. Nanga ndi uthenga uti wa Mulungu
ndi chivumbulutso chake chiti chomwe iwo akhoza
kukhulupirira?
7. Tsoka kwa wochimwa aliyense wabodza!. 8. Amene
amamva mawu a Mulungu amene ali kunenedwa kwa iye
ndipo amapitirizabe kunyada ngati iye sanamve. Motero
muuze iye za chilango chowawa! 9. Ndipo pamene iye
akamva mawu a Mulungu, amawasandutsa kukhala
masewera. Ndipo kwa otere kudzakhala chilango
chochititsa manyazi. 10. Kutsogolo kwawo kuli Gahena,
ndipo sadzapeza phindu lina lililonse pa ntchito zawo

kapena kwa iwo amene adawasandutsa kukhala wowasamala
poonjezera pa Mulungu. Ndipo iwo adzalandira chilango
chowawa. 11. Ichi ndi chilangizo choona. Ndipo iwo
amene amakana zizindikiro za Ambuye wawo, adzalandira
chilango chapadera chowawa.
12. Ndi Mulungu amene adachepetsa mphamvu ya nyanja
kuti masitima aziyenda mwaulamuliro wake ndipo kuti
inu mukhoza kufuna chisomo chake kuti muzimuthokoza.
13. Ndipo Iye adachepetsa mphamvu ya chinthu chilichonse
chimene chili kumwamba ndi dziko lapansi. Ndithudi mu
zimenezi muli zizindikiro kwa anthu amene amaganiza
mofatsa.
14. Auze iwo amene amakhulupirira kuti akhululukire iwo
amene sakhulupirira m'masiku a Mulungu kuti Iye akhoza
kulipira anthu chimene amachita. 15. Aliyense amene
amachita zabwino amachitira mzimu wake ndipo aliyense
amene amachita zoipa adzilakwira yekha. Pomaliza nonse
mudzabwerera kwa Ambuye wanu.
16. Ndithudi Ife tidawapatsa ana a Israyeli Buku ndi
luntha lozindikira mawu a Mulungu ndi Utumwi ndipo
tidawapatsa zinthu zokoma ndipo tidawakonda iwo
kuposa mitundu ina yonse. 17. Ndipo Ife tidawapatsa
zizindikiro zooneka za chipembedzo. Ndipo iwo
adayamba mipatuko pamene nzeru zidaperekedwa kwa
iwo chifukwa cha njiru pakati pawo. Ndithudi Ambuye
wako adzaweruza pakati pawo pa tsiku lachiweruzo pa
nkhani zimene anali kutsutsana. 18. Ndipo iwe takuika pa
njira yoyenera. Motero tsatira yoyenerayo ndipo usatsatire
zilakolako za iwo amene sadziwa chilichonse. 19. Ndithudi
iwo sangakuthandize chilichonse ku mkwiyo wa Mulungu.

Ndi anthu oipa okha okha omwe amakhala ngati atetezi a wina ndi mnzake koma Mulungu ndi Mtetezi wa iwo amene amalewa zoipa. [20.] Uwu ndi umboni womveka kwa anthu ndi langizo ndi chisomo kwa anthu amene ali ndi chikhulupiriro chokhazikika.

[21.] Kodi anthu amene amachita zoipa amaganiza kuti Ife tidzawasamala monga mmene tidzasamalire anthu amene amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino zofanana ndi moyo wawo ndiponso imfa yawo? Iwo amaweruza molakwa. [22.] Ndipo Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi mwachoonadi kuti mzimu uliwonse ukhoza kupeza dipo lake molingana ndi zimene udachita ndipo palibe amene adzaponderezedwa.

[23.] Kodi wamuona iye amene amasandutsa zilakolako zake kukhala mulungu wake? Mulungu wamusocheretsa iye ndipo wakhazikitsa chophimba m'makutu mwake ndi mu mtima mwake. Ndipo waika chophimba m'maso mwake? Kodi ndani amene akhoza kumutsogolera iye kupatula Mulungu? Kodi tsopano simudzakumbukira?

[24.] Ndipo iwo amati, "Kulibe china chilichonse kupatula moyo wathu wa pa dziko lapansi. Ife timakhala ndi moyo ndipo timafa ndipo palibe chimene chimationonga ife koma nthawi yokha ndiyo." Ndipo iwo sadziwa chilichonse cha izo koma amangonena zongoganiza. [25.] Ndipo pamene chivumbulutso chathu chomveka chimanenedwa kwa iwo, mtsutso wawo siukhala wina koma kuti, "Bweretsa makolo athu akale ngati zimene ukunena ndi zoonadi." [26.] Nena: "Mulungu amakupatsani inu moyo, amakuphani ndipo Iye adzakusonkhanitsani pa tsiku la kuuka kwa akufa limene lilibe chikayiko. Koma ambiri sadziwa zimenezi."

27. Mulungu! Wake ndi ufumu wakumwamba ndi dziko
lapansi. Ndipo patsiku limene ola lidzadza, onse amene
amanena zinthu zabodza adzataya chilichonse. 28. Ndipo iwe
udzaona mtundu uliwonse utagwada pansi ndipo mtundu
uliwonse udzaitanidwa monga mmene zidalembedwera.
Lero mudzalipidwa molingana ndi zimene mudachita.
29. Buku lathuli lili kunena za inu mwachilungamo.
Ndithudi timalemba zonse zimene mumachita.
30. Ndipo iwo amene adakhulupirira ndipo amachita
ntchito zabwino, Ambuye wawo adzawalowetsa m'chisomo
chake. Kumeneku ndiko kupambana kwenikweni.
31. Koma iwo amene sadakhulupirire adzauzidwa kuti,
"Kodi chivumbulutso changa sichidalakatulidwe kwa inu?
Koma inu munali onyada ndipo munali anthu ochita zoipa."
32. Ndipo pamene zidanenedwa kuti, "Ndithudi lonjezo la
Mulungu ndi loona ndipo palibe zokayikitsa za kudza kwa
Ola", inu mudati, "Ife sitidziwa kuti Ola ndi chiyani ndipo
ife sitiliganiza kupatula kuti ndi maganizo opanda pake
ndipo ife sitilikhulupirira ayi."
33. Ndipo zoipa zonse zimene adachita zidaonekera poyera
kwa iwo ndipo zonse zimene anali kunyoza zidzawapeza!
34. Ndipo kudzanenedwa kuti, "Lero takuiwalani inu monga
momwe inu mudaiwalira za tsiku lanuli. Ndipo malo anu
okhala ndi ku Moto ndipo kumeneko sikudzakhala wina
wokuthandizani." 35. "Ichi ndi chifukwa chakuti mudatenga
chivumbulutso cha Mulungu ngati chinthu choseweretsa
ndipo moyo wa padziko lino lapansi udakunyengani inu."
Motero patsiku limeneli, iwo sadzachotsedwa ndipo
sadzaloledwa kukonza zolakwa zawo.
36. Motero kuyamikidwa konse kukhale kwa Mulungu,

Ambuye wa Kumwamba ndi Ambuye wa padziko lapansi
ndi Ambuye wa zolengedwa zonse. 37. Ndipo wake ndi
Ufumu wakumwamba ndi padziko lapansi ndipo Iye ndi
Wopambana ndi Wanzeru zonse.

Sura 46 • Al-Ah'kâf

# AL AHQAF

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. *Ha Mim*.

2. Chivumbulutso cha Buku chochokera kwa Mulungu,
wamphamvu ndi waluntha. 3. Ife sitidalenge kumwamba
ndi dziko lapansi ndi zonse zimene zili m'menemo
kupatula ndi choonadi ndipo kuti zikhale mpaka pa nthawi
yotsimikizidwa. Koma onse amene sakhulupirira samvera
zimene achenjezedwa.
4. Nena, "Kodi mudayamba mwaganiza za zimene
mumapembedza zoonjezera pa Mulungu? Ndilangizeni
za zimene zidalenga padziko lapansi? Kapena kodi izo zili
ndi gawo m'zinthu zimene zili kumwamba? Bweretsani
kwa ine Buku limene lidalipo ili lisanadze kapena
nzeru zina zotsatira ngati inu muli kunena zoonadi."
5. Kodi wosochera kwambiri ndani kuposa iye amene
amapembedza kuonjezera pa Mulungu chinthu chimene
sichingathe kumuyankha mpaka patsiku lachiweruzo
ndipo sichikumva zimene ali kuchifunsa? 6. Ndipo pamene

mtundu wa anthu udzasonkhanitsidwa, izo zidzawaukira
iwo ndikukana kuti iwo sanali kuzipembedza izo.
7. Ndipo pamene chivumbulutso chathu chomveka
chimawerengedwa kwa iwo, anthu osakhulupirira amanena
za choonadi pamene chidza kwa iwo kuti "Awa ndi matsenga
oonekera poyera." 8. Kapena iwo amati, "Wapeka yekha?"
Nena, "Ngati ine ndapeka ndekha, inu mulibe mphamvu
yonditeteza ine kwa Mulungu. Iye ali kudziwa bwino
chilichonse chimene mumanena chokhudza chimenechi.
Iye ndi wokwana kukhala mboni pakati pa ine ndi inu ndipo
Iye ndi wokhululukira ndiponso Mwini chisoni chosatha."
9. Nena, "Ine sindine woyamba mwa Atumwi ndipo
sindidziwa chimene chingachitike kwa ine kapena kwa
inu. Ine sinditsatira china chilichonse kupatula chokhacho
chimene chavumbulutsidwa kwa ine. Ndipo ine sindili
wina aliyense koma Mchenjezi basi." 10. Nena: "Tandiuzani!
Ngati uthengawu ndi wochokera kwa Mulungu ndipo inu
muli kukana kukhulupirira pamene mboni yochokera
pakati pa ana a Israyeli yatsimikizira kuti Koraniyi ndi
yochokera kwa Mulungu ndipo ndi yofanana. Motero
iye adakhulupirira pamene inu muli kunyada. Ndithudi
Mulungu satsogolera anthu ochita zoipa."
11. Ndipo anthu osakhulupirira amanena zokhudza anthu
okhulupirira kuti, "Ngati uthengawu ukadakhala wabwino,
iwo sakadaulandira msanga kuposa ife. Ndipo popeza
iwo safuna kuti atsogozedwe ndi uthengawu iwo amati,
"Limeneli ndi bodza chabe la anthu akale."
12. Ndipo lisanadze Bukuli padali Buku la Mose limene
lidali ulangizi ndi chisomo. Ndipo Buku ili lili kutsimikiza za
ilo m'chinenero cha Chiarabu kuchenjeza anthu ochimwa

ndi kufotokoza nkhani zabwino kwa iwo amene amachita
zabwino. 13. Ndithudi onse amene amati, "Ambuye wathu
ndi Mulungu"; ndipo amapitirira kuchita ntchito zabwino,
iwo sadzaopa china chilichonse kapena kudandaula. 14. Awa
ndiwo amene adzakhala ku Paradiso mpaka kalekale ngati
malipiro a zonse zimene adachita.

15. Ndipo Ife tidalamula munthu kuti azichita zabwino
kwa makolo ake. Amayi ake amavutika pomubereka ndi
pomulera iye. Ndipo kuyambira pamene waberekedwa ndi
pamene asiya kuyamwa ndi miyezi makumi atatu. Patapita
nthawi iye amakula ndipo akakwanitsa zaka makumi anayi
amati, "Ambuye wanga! Ndipatseni mphamvu ndi nzeru
kuti ndikhale woyamika chifukwa cha chisoni chimene
mwandionetsera ndi chimene mwaonetsera kwa makolo
anga kuti ndizichita zabwino zimene zidzakukondweretsani
Inu. Ndipo chitireni zabwino zokhudza ana anga. Ndithudi
ine ndiyang'ana kwa Inu polapa ndipo, ndithudi, ine
ndine mmodzi wa anthu ogonjera." 16. Awa ndiwo amene
tidzalandira zabwino za ntchito zawo ndi kuwakhululukira
zoipa zawo. Iwo adzakhala m'gulu la anthu a ku Paradiso.
Lonjezo loona, limene lidalonjezedwa kwa iwo.

17. Koma yense amene amanena kwa makolo ake kuti,
"Asa! Kodi inu muli kundilonjeza kuti ine ndidzaukitsidwa
pamene mibadwo ina yambiri idapita kale ine
ndisanabadwe?" Ndipo iwo amapempha chithandizo cha
Mulungu nati, "Tsoka kwa iwe! Khulupirira! Ndithudi
lonjezo la Mulungu ndi loona." Koma iye amati, "Ichi si
chinthu china koma nkhani zachabe za anthu amakedzana."
18. Awa ndiwo amene mawu a chilango adatsimikiziridwa

pakati pa mitundu yakale ya majini ndi anthu amene
adapita kale. Ndithudi iwo ndi otayika.
19. Ndipo kwa onse kudzakhala miyeso yolingana ndi
zimene adachita kuti Iye akhoza kuwalipira zochita zawo
mosanyenga ndipo iwo sadzaponderezedwa. 20. Ndipo
pa tsiku limene iwo osakhulupirira adzatengedwa kupita
ku moto kudzanenedwa kuti, "Inu mudalandira zokoma
zanu pamene munali padziko lapansi ndipo munali
kusangalala zedi. Koma lero mudzakhaulitsidwa ndi
chilango chochititsa manyazi chifukwa cha mwano umene
mumachita padziko lapansi popanda chifukwa, ndipo
mudapitirirabe kuswa malamulo."
21. Kumbukira za m'bale wa anthu a mtundu wa Aad
pamene iye adawachenjeza anthu ake m'chipululu.
Ndithudi kudali Achenjezi ena iye asanabadwe ndi
atachoka amene amati, "Musapembedze wina aliyense
kupatula Mulungu chifukwa ndiopa chilango chowawa
chimene chingadze pa inu patsiku lachiweruzo." 22. Iwo
adati, "Kodi iwe wadza ndi cholinga chotiletsa ife kuti
tisapembedze milungu yathu? Choncho bweretsa kwa ife
mavuto amene uli kutiopseza nawo ngati iwe uli kunenadi
zoona." 23. Iye adati, "Amadziwa zonse ndi Mulungu ndipo
ine ndingokuuzani uthenga umene wanditumа koma ine
ndikuona kuti inu ndinu anthu amwano."
24. Ndipo pamene adachiona icho ngati mtambo woyera
kuchokera kumwamba kupita ku madambo, iwo adati,
"Uwu ndi mtambo umene udzatibweretsera ife mvula."
"Iyayi. Ili ndi tsoka limene mumafuna kuti lidze msanga
kwa inu. Ndi mphepo ya mkuntho m'mene muli chilango
choopsa." 25. Kuononga chinthu chilichonse ndi mphamvu

ya Ambuye wake. Ndipo pamene kumacha m'mawa
padalibe china chilichonse chooneka kupatula mabwinja
a nyumba zawo. Mmenemo ndi mmene timalangira anthu
ochita zoipa.
26. Ndipo, ndithudi, tidawapanga iwo kukhala amphamvu
zoposa zanu. Ndipo Ife tidawapatsa makutu, maso ndi
mitima koma palibe china chilichonse chimene makutu
awo, maso awo ndi mitima yawo idawathandiza chifukwa
iwo adakana kumvera chivumbulutso cha Mulungu
ndipo icho chimene anali kuchinyoza chidawapeza iwo.
27. Ndithudi Ife taononga mizinda imene yakuzungulirani
inu ndipo tili kubwereza chivumbulutso chathu kuti mwina
akhoza kutembenuka. 28. Nanga ndi chifukwa chiyani
sadathandizidwe ndi iwo amene anali kuwapembedza ngati
milungu yoonjezera pa Mulungu weniweni ndi cholinga
chakuti iwabweretse kufupi ndi Mulungu? Iyayi. Iyo
idawasiya padzuwa. Ndipo ilo linali bodza lomwe iwo anali
kupeka.
29. Ndi pamene Ife tidatumiza kwa iwe, gulu la majini
limene lidadzamvetsera Korani, ndipo pamene iwo
adaimirira pakati pawo adati, "Khalani chete!" Ndipo
pamene atatha kumvetsera, iwo adabwerera kwa anthu
awo ngati ochenjeza. 30. Iwo adati, "Oh inu anthu athu! Ife
tamva mawu a m'Buku limene lavumbulutsidwa pambuyo
pa Mose limene litsimikizira zimene zidavumbulutsidwa
kale zotsogolera anthu ku choonadi ndi kunjira yoyenera."
31. Oh anthu athu! Vomerani kuitana kwa iye amene
akuitanirani ku njira ya Mulungu ndipo mukhulupirire
mwa iye. Mulungu adzakukhululukirani machimo anu ndi
kukupulumutsani inu kuchilango chowawa. 32. Ngati wina

safuna kumvera Mtumwi wa Mulungu, iye sadzathawa sadzathawa chikonzero cha Mulungu cha padziko lapansi ndipo sadzapeza wina womuteteza kupatula Mulungu. Otere ndi olakwa kwambiri.

33. Kodi iwo saona kuti Mulungu, amene adalenga kumwamba ndi dziko lapansi, sadatope chifukwa cha ntchito yolengayi ndipo kuti ali ndi mphamvu yopereka moyo kwa akufa? Inde! Ndithudi Iye ali ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse. 34. Ndipo patsiku limene onse osakhulupirira adzaonetsedwa moto, iwo adzafunsidwa kuti, "Kodi ichi si choonadi?" Iwo adzati, "Inde pali Ambuye wathu!" Ndipo Iye adzati, "Tsopano lawani chilango chimene inu munali kunena kuti ndi bodza."

35. Motero pirira monga momwe Atumwi akale opirira anali kuchitira ndipo usafune kuti chilango chawo chidze pa iwo mwamsanga. Patsiku limene iwo adzaona zimene ali kulonjezedwa, iwo adzaoneka ngati kuti adangokhala padziko lapansi ola limodzi lokha. Udindo wako ndi kupereka uthenga. Palibe wina amene adzaonongeke kupatula yekhayo amene amaswa malamulo.

Sura 47 • Muhammad

# Muhammad

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Iwo amene sakhulupirira ndipo amaletsa anzawo kutsatira njira ya Mulungu, Iye adzasandutsa ntchito

zawo kukhala zopanda pake. 2. Koma iwo amene
amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino, ndipo
amakhulupirira mu chivumbulutso chimene chatumizidwa
kwa Muhammad, chifukwa icho ndi choonadi chochokera
kwa Ambuye wawo, Iye adzawachotsera zoipa ndi
kulongosola machitidwe awo. 3. Ichi ndi chifukwa chakuti
onse amene sakhulupirira amatsatira zabodza pamene iwo
amene amakhulupirira amatsatira choonadi chochokera
kwa Ambuye wawo. Mmenemo ndi mmene Mulungu
amaonetsera zitsanzo zake kwa anthu.

4. Motero pamene inu mukumana ndi anthu
osakhulupirira pa nkhondo, thyolani makosi awo, mpaka
pamene mukupha ndi kuvulaza ambiri ndipo muwagwire
kukhala akaidi ndipo pambuyo pake mukhoza kuwamasula
powaonetsa chisoni kapena akhale ngati chigwiriro mpaka
pamene nkhondo itatha. Motero inu mwalamulidwa.
Koma chikadakhala chifuniro cha Mulungu, ndithudi,
Iye Mwini wake akadawapatsa chilango chowayenera.
Koma Iye wafuna kuti inu mumenyane nawo ndi cholinga
chokuyesani wina ndi mnzake. Koma iwo amene aphedwa
m'njira ya Mulungu, Iye sadzalola kuti ntchito zawo zipite
pachabe. 5. Iye adzawatsogolera ndi kulemekeza malo awo.
6. Iye adzawalowetsa ku Paradiso kumene adawalonjeza
kale.

7. Oh inu anthu okhulupirira! Ngati inu muthandiza
m'ntchito za Mulungu, Iye adzakuthandizani inu ndipo
adzakulimbikitsani. 8. Koma iwo amene sakhulupirira,
kwa iwo kuli chionongeko ndipo Mulungu adzapanga
kuti ntchito zawo zonse zikhale zopanda phindu. 9. Ichi
ndi chifukwa chakuti iwo amadana ndi chivumbulutso

cha Mulungu, ndipo Iye wapanga ntchito zawo kukhala zopanda pake. 10. Kodi iwo sadayende padziko lapansi ndi kuona zimene zidawachitikira iwo amene adalipo kale? Mulungu adaponya chiononongeko pa iwo ndipo onse osakhulupirira adzaona mavuto a mtundu womwewo. 11. Ichi ndi chifukwa chakuti Mulungu ndi Mtetezi wa iwo amene amakhulupirira pamene anthu osakhulupirira alibe wowateteza.

12. Ndithudi Mulungu adzalowetsa ku minda imene pansi pake pamayenda mitsinje yamadzi onse amene amakhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino. Pamene onse amene sakhulupirira ndipo amadzisangalatsa ndi kudya ngati momwe zimadyera nyama kumoto ndiko kudzakhala malo awo okhala. 13. Ndi mizinda yambiri imene idali ndi mphamvu zoposa Mzinda umene wakupirikitsa iwe imene Ife tidaiononga. Ndipo padalibe wina wowathandiza.

14. Kodi iye amene watsogozedwa bwino ndi Ambuye wake ndi wofanana ndi iwo amene ntchito zawo zoipa zimaoneka ngati zabwino ndipo amatsatira zilakolako zawo zopanda pake? 15. Mwaonekedwe amunda umene iwo amene amalewa zoipa alonjezedwa ndi akuti m'menemo muli mitsinje yamadzi amene sakuphwa ndi mitsinje yamkaka umene siusintha kukoma kwake, ndipo mitsinje ya vinyo ndi mitsinje ya uchi wabwino. Imo muli zipatso zosiyanasiyana ndi chikhulupiriro chochokera kwa Ambuye wawo. Kodi awa ali ngati iwo amene adzakhala kumoto mpaka kalekale ndipo amapatsidwa madzi ogaduka amene amaboola m'matumbo?

16. Ndipo pakati pawo pali iwo amene amamva zimene iwe umanena, mpaka pamene akusiya iwe, iwo amati

kwa amene adapatsidwa nzeru, “Kodi ndi chiyani chimene wanena posachedwapa?” Awa ndiwo amene mitima yawo yatsekedwa ndi Mulungu ndipo amatsatira zilakolako zopanda pake. [17.] Pamene iwo amene amatsatira njira yoyenera, Iye amawatsogolera ndi kuwonjezera chikhulupiriro chawo.

[18.] Kodi iwo akudikira china kuposa Ola kuti lidze kwa iwo mwadzidzidzi? Koma zizindikiro zina zadza kale, ndipo chitadza pa iwo, kodi iwo adzapindula chiyani ndi chikumbutso? [19.] Motero dziwani kuti kulibe mulungu wina koma Mulungu weniweni ndipo pempha chikhululukiro chako ndi cha amuna ndi akazi amene amakhulupirira. Ndipo Mulungu amadziwa mmene inu mumayendera ndi mmene mumakhalira m’nyumba zanu.

[20.] Iwo amene amakhulupirira amati, “Kodi bwanji Mutu wina siudavumbulutsidwe?” Koma pamene mutu wotsimikiza uvumbulutsidwa ndipo kumenya nkhondo kulamulidwa mmenemo iwe udzaona iwo amene m’mitima mwawo muli matenda ali kukuyang’ana iwe ngati munthu amene ali kukomoka pamene imfa ili kudza kwa iye. Koma zinali bwino kwa iwo. [21.] Kumvera ndi mau abwino (zikadakhala zinthu zabwino). Ndipo pamene nkhani iweruzidwa, ndipo iwo akadadzipereka mwachoonadi kwa Mulungu, ndithudi, zikadakhala zabwino kwa iwo. [22.] Kodi ngati inu mukadapatsidwa udindo wolamulira, mukadachita zinthu zoipa padziko ndi kuphwanya ubale wanu ndi anthu a mtundu wanu? [23.] Amenewa ndiwo amene Mulungu wawatemberera ndipo Iye wawapanga iwo kukhala osamva ndi akhungu.

[24.] Kodi iwo sangaganize za uthenga wa m’Korani?

Kodi kapena mitima yawo ndi yotsekedwa? 25. Ndithudi
iwo amene amabwerera m'mbuyo ndi kukhalanso
osakhulupirira pamene atalandira kale ulangizi,
amatsogozedwa ndi Satana amene amawanamiza ndi
zinthu zopanda pake. 26. Ichi ndi chifukwa chakuti iwo
amanena kwa iwo amene amadana ndi zimene Mulungu
wavumbulutsa kuti, "Ife tidzakumverani mu zina za nkhani
zimenezi." Koma Mulungu amadziwa zinsinsi zawo zonse.
27. Kodi iwo adzachita chiyani pamene angelo adzalanda
miyoyo yawo ndi kuwamenya pa nkhope ndi m'misana
yawo? 28. Ichi ndi chifukwa chakuti iwo amatsatira zinthu
zimene zimakwiyitsa Mulungu ndipo amadana ndi zimene
zimamukondweretsa Iye. Kotero Mulungu adasandutsa
ntchito zawo kukhala zinthu zopanda pake.

29. Kodi iwo amene m'mitima mwawo muli matenda
amaganiza kuti Mulungu sadzaulula zoipa zawo
zonse? 30. Ife tikadafuna tikadakuonetsa iwe ndipo iwe
ukadawadziwa chifukwa cha zizindikiro zawo ndipo,
ndithudi, udzawadziwa chifukwa cha mayankhulidwe awo.
Mulungu amadziwa ntchito zanu.

31. Ndithudi Ife tidzakuyesani mpaka pamene tiyesa
onse amene amalimbikira kwambiri ndi iwo amene
opirira ndipo Ife tidzayesa ntchito zanu. 32. Ndithudi iwo
amene sakhulupirira ndipo amaletsa anthu kutsata njira
ya Mulungu ndipo amatsutsana ndi Mtumwi pamene
atalandira kale langizo loyenera, iwo sangathe kugonjetsa
Mulungu mwanjira ina iliyonse. Koma Iye adzafafaniza
ntchito zawo zonse ndi kuzisandutsa kukhala zopanda
pake.

33. Oh inu anthu okhulupirira! Mverani Mulungu

ndipo mverani Mtumwi wake ndipo musasandutse
ntchito zanu kukhala zopanda pake. 34. Ndithudi onse
amene sakhulupirira ndipo amaletsa anthu kutsatira
njira ya Mulungu, ndipo amafa ali osakhulupirira
Mulungu sadzawakhululukira. 35. Motero inu musafoke
ndipo musafunse kuti kukhale mtendere pamene muli
kupambana. Mulungu ali ndi inu ndipo Iye sadzapungula
mphotho ya ntchito zanu zabwino.
36. Moyo wa pa dziko lino ndi masewera enieni ndiponso
kotayira nthawi koma ngati inu mukhulupirira ndi kulewa
machimo, Iye adzakulipirani inu ndipo sadzakufunsani za
katundu amene muli naye. 37. Ngati Iye akadakufunsani
za katundu wanu ndi kukuumirizani, ndithudi, inu
mukadachita umbombo ndipo Iye adzaulula zinsinsi zanu
zonse. 38. Taonani! Inu ndinu amene mwaitanidwa kupereka
m'njira ya Mulungu koma pakati panu pali anthu omwe
ndi mbombo. Ndipo aliyense amene achita umbombo
amadzimana yekha. Mulungu sasowa kanthu pamene
inu ndinu osauka. Ndipo ngati inu mubwerera m'mbuyo
Iye adzaika m'malo mwanu anthu ena ndipo sadzakhala
olingana ndi inu.

# AL FATEH

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ndithudi Ife takupambanitsa iwe,kupambana
kwenikweni. 2. Kuti Mulungu akukhululukire machimo
ako akale ndi am'tsogolo omwe, ndi kumaliza ubwino wake
pa iwe ndi kukutsogolera ku njira yoyenera. 3. Ndikuti
Mulungu athe kukuthandiza ndi chithandizo chokwanira.
4. Ndiye amene adatumiza chisomo m'mitima mwa
anthu okhulupirira kuti chikhulupiriro chawo chikhoza
kukhala chokhazikika za Mulungu ndi zonse zimene zili
kumwamba ndi padziko lapansi. Ndipo Mulungu ndi
wodziwa ndi walunthа. 5. Kuti akhoza kulowetsa amuna
ndi akazi okhulupirira ku minda imene pansi pake pali
mitsinje yamadzi oyenda kuti akhale komweko mpaka
kalekale ndi kuwakhululukira machimo awo ndipo pamaso
pa Mulungu, ndiko kupambana kwenikweni kumeneku.
6. Ndipo akhoza kulanga anthu a chinyengo, aamuna ndi
aakazi ndi anthu opembedza mafano, amuna ndi akazi
amene amaganiza zoipa za Mulungu. Kwa iwo kudzadza
mavuto ndipo mkwiyo wa Mulungu uli pa iwo. Iye
wawatemberera iwo ndipo wakonzekera Gahena omwe ndi
malo oipa kukhalako. 7. Mulungu zake ndi zonse zimene zili
kumwamba ndi pa dziko lapansi. Mulungu ndi wamphamvu
ndi wa nzeru.
8. Ndithudi takutumiza iwe ngati Mboni, ngati

Wolalikira uthenga wabwino ndiponso ngati Mchenjezi.
9. Ndi cholinga chakuti inu anthu mukhoza kukhulupirira
mwa Mulungu ndi Mtumwi wake ndi kuti mumuthandize
ndi kumulemekeza iye ndipo kuti muzilemekeza Mulungu
m'mawa ndi madzulo. 10. Ndithudi onse amene amalumbira
kuti ali pambuyo pako, iwo amalumbira kuti ali pambuyo
pa Mulungu. Ndipo dzanja la Mulungu ndi loposa manja
awo. Ndipo aliyense amene aphwanya lonjezo lake,
Iye akungodziponderezа yekha ndipo aliyense amene
akwaniritsa lonjezo limene adachita ndi Mulungu, Iye
adzamulipira iye mphotho yopambana.
11. Maarabu okhala m'chipululu amene adatsalira
m'mbuyo adzati kwa iwe, "Ife tidatangwanika ndi chuma
ndi mabanja athu, motero tipemphere chikhululukiro." Iwo
amangonena ndi milomo yawo zimene m'mitima mwawo
mulibe. Nena, "Kodi ndani angakuyankhulireni inu kwa
Mulungu ngati Iye atafuna kukuonongani kapena atafuna
kuti akuchitireni zabwino? Iyayi, Mulungu amadziwa
zonse zimene mumachita." 12. Iyayi! Inu munali kuganiza
kuti Mtumwi pamodzi ndi onse okhulupirira sadzabwerera
ku mabanja awo ndipo zimenezo zinali zokusangalatsani
inu ndipo inu munali kuganiza maganizo oipa ndipo inu
munali anthu opanda pake opita ku chionongeko. 13. Ndipo
aliyense amene sakhulupirira mwa Mulungu ndi Mtumwi
wake, ndithudi, Ife tawakonzera anthu osakhulupirira
moto woyaka. 14. Wa Mulungu ndi Ufumu wakumwamba
ndi padziko lapansi. Iye amakhululukirira amene
wamufuna ndipo amalanga aliyense amene wamufuna.
Ndipo Mulungu ndi wokhululukira nthawi zonse ndi
Mwini chisoni chosatha.

15. Iwo amene adatsala m'mbuyo adzati, pamene adzaona
inu muli kukonzeka kukatenga katundu amene mwapeza
pa nkhondo, "Tiloleni kuti tipite nanu." Iwo afuna kusintha
mawu a Mulungu. Nena, "Ndikosatheka! Inu simudzapita
nafe. Mulungu ananena kale za inu." Ndipo iwo adzati,
"Iyayi! Inu muli kutichitira ife nsanje." "Iyayi! Koma iwo
sazindikira koma pang'ono pokha."
16. Nena kwa iwo amene amakhala m'chipululu ndipo
adakhalira m'mbuyo kuti, "Inu mudzaitanidwa, kuti
mumenyane ndi anthu amphamvu kwambiri ndipo
inu mudzamenyana nawo mpaka pamene adzagonja.
Ndipo ngati inu mumvera, Mulungu adzakulipirani
mphotho ya mtengo wapatali ndipo ngati inu muthawa,
Iye adzakulangani inu ndi chilango chowawa." 17. Palibe
cholakwa kapena mlandu kwa wakhungu, kapena
cholakwa kapena mlandu kwa wopunduka ndipo palibe
cholakwa kapena mlandu kwa wodwala ngati iwo sapita
nawo. Aliyense amene amvera Mulungu ndi Mtumwi wake,
Mulungu adzamulandira ku minda imene ili ndi mitsinje
yoyenda madzi pansi pake ndipo aliyense amene athawa,
Mulungu adzamulanga ndi chilango chowawa.
18. Ndithudi Mulungu adasangalala ndi anthu
okhulupirira pamene iwo adakulonjeza patsinde pa mtengo
kuti adzakhala ndi iwe ndipo Iye adadziwa zimene zidali
m'mitima mwawo. Ndipo Iye adatumiza madalitso kwa
iwo ndipo adawalipirira mwamsanga mphotho yopambana.
19. Ndipo iwo adzalanda katundu wambiri. Ndipo Mulungu
ndi Wamphamvu ndi Waluntha. 20. Mulungu wakulonjeza
katundu wambiri amene udzalandira ndipo wakupatsiratu,
ndipo Iye wamanga manja ya anthu kuti asakukhudze, kuti

chikhale chizindikiro kwa anthu okhulupirira ndipo kuti
Iye akutsogolere ku njira yoyenera. 21. Ndi zina zomwe iwe
siudazipeze ndithudi,Mulungu wazizungulira. Mulungu ali
ndi mphamvu pa chinthu china chilichonse.

22. Ngati anthu osakhulupirira amenyana nanu, ndithudi,
iwo adzathawa, ndipo iwo sadzapeza wina aliyense
wowateteza kapena kuwathandiza. 23. Amenewa ndiwo
machitidwe a Mulungu kuyambira kalekale. Ndipo inu
simudzapeza chosintha m'machitidwe a Mulungu. 24. Ndipo
ndiye amene adamanga manja awo kuti asakukhudzeni inu
ndipo manja anu kuti asawakhudze iwo m'kati mwa Makka
pamene Iye adakupambanitsani inu. Ndipo Mulungu
amaona zonse zimene mumachita.

25. Iwo ndiwo amene sadakhulupirire ndipo
adakutchingani kuti musalowe mu Mzikiti Wolemekezeka
ndi kukuletsani kuti nyama za nsembe zisakafike pa malo
operekerapo nsembe. Koma pakadakhala kuti panalibe
anthu aamuna okhulupirira ndi aakazi okhulupirira, amene
simuwadziwa, inu mukadawapondereza kotero kuti china
chake choipa chikadadza pa inu chifukwa cha iwo, kuti
Mulungu aonetse chisomo chake kwa aliyense amene Iye
wamufuna. Koma iwo akadapatukana wina ndi mnzake,
Ife ndithudi tikadalanga ndi chilango choopsa onse amene
sadakhulupirire amene anali pakati pawo.

26. Pamene iwo osakhulupirira adasunga chidani
m'mitima mwawo, chidani cha nthawi ya chikunja, ndipo
Mulungu adatumiza chisomo chake kwa Mtumwi wake ndi
kwa anthu okhulupirira. Ndipo adawachititsa iwo kukhala
omvera malamulo odziletsa ndipo adakhazikitsa bata

kukhala pa iwo chifukwa adali oyenera kulilandira batalo. Ndipo Mulungu amadziwa chinthu china chilichonse.

27. Ndithudi Mulungu adzakwaniritsa masomphenya a Mtumwi wake. Ndithudi inu mudzalowa mu Mzikiti Wolemekezeka, ngati Mulungu afuna mopanda vuto ndipo ena adzameta mitu yawo ndiponso ena adzapungula tsitsi lawo ndipo mudzakhala opanda mantha. Iye adadziwa zimene inu simudadziwe ndipo adapereka moonjezera pa zimenezi, kupambana kwa msanga.

28. Ndiye amene adatumiza Mtumwi wake ndi ulangizi ndiponso chipembedzo choonadi. Ndipo Iye wachipanga icho kuti chikhale chopambana zipembedzo zina zonse. Ndipo Mulungu ndi wokwana kukhala mboni.

29. Muhammad ndi Mtumwi wa Mulungu ndipo onse amene amamutsatira iye amakhala olimbika polimbana ndi anthu osakhulupirira koma amachitirana chisoni wokhaokha. Inu mumawaona ali nkupembedza pa mawondo awo ndi kugwetsa mphumi zawo kufunafuna chisomo chochokera kwa Mulungu ndi chisangalalo chake. Pamphumi pawo pali zizindikiro zimene zimadza chifukwa chakugunditsa mphumi zawo pansi. Awa ndi maonekedwe awo amene ali m'Chipangano Chakale. Koma maonekedwe awo amene ali mu Chipangano Chatsopano ali monga momwe mbewu imatulutsira nsonga yake ndi kuikhwimitsa. Ndipo iyo imalimba ndi kukhala yoimirira modabwitsa ndi kusangalatsa amene adaibzala. Kuti Iye akwiyitse osakhulupirira ndi izo. Mulungu walonjeza chikhululukiro ndi mphotho yaikulu kwa anthu okhulupirira ndiponso ochita ntchito zabwino.

# Al Hujurat

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Oh inu anthu okhulupirira! Musadzikweze pamaso pa
Mulungu ndi pa Mthenga wake, koma opani Mulungu
chifukwa Iye ndiye amene amamva ndi kudziwa chinthu
china chilichonse.
2. Oh inu anthu okhulupirira! Musakweze mawu anu
kuposa a Mtumwi ndipo musayankhule ndi mawu okweza
kwa iye monga momwe mumachitira mukamayankhulana
nokhanokhanu chifukwa ntchito zanu zingasanduke
zopanda pake pamene inu simuli kudziwa. 3. Ndithudi
iwo amene amayankhula motsitsa pamaso pa Mtumwi
wa Mulungu ndiwo amene Mulungu wayesa mitima yawo
kuti ndi yabwino, ndipo iwo adzalandira chikhululukiro
ndi mphotho yaikulu. 4. Ndithudi iwo amene amafuulira
iwe kunja kwa zipinda, onse alibe nzeru. 5. Iwo akadapirira
mpaka pamene iwe udza kwa iwo, ndithudi, zikadakhala
bwino ndipo Mulungu ndi wokhululukira ndi wachisoni
chosatha.
6. Oh inu anthu okhulupirira! Ngati munthu wochita
zoipa adza kwa inu ndi nkhani, ifufuzeni poyamba
chifukwa mwina mukhoza kupweteka anthu mosadziwa
ndi kuyamba kumva chisoni pambuyo pake chifukwa
cha zimene mwachita. 7. Ndipo dziwani kuti pakati panu
pali Mtumwi wa Mulungu ndipo iye akamachita zimene

mufuna, ndithudi, inu mukadavutika kwambiri. Koma
Mulungu wakusungitsani inu chipembedzo chake ndipo
wachipanga icho kukhala chokongola m'mitima mwanu,
ndi kupanga kusakhulupirira kukhala chinthu choipa
ndiponso kuswa malamulo ndi kusamvera. Awa ndiwo
amene amatsatira njira yoyenera. 8. Chisomo ndi chifundo
chochokera kwa Mulungu. Ndipo Mulungu amadziwa
chinthu china chilichonse ndipo ndi wanzeru kwambiri.

9. Ngati magulu awiri ochokera kwa anthu okhulupirira
amenyana, khazikitsa mtendere pakati pawo. Koma
ngati gulu lina liswa malamulo mopyola muyeso, nonse
menyanani nalo gulu lotero mpaka pamene limvera
lamulo la Mulungu. Ndipo ngati ilo limvera, khazikitsani
mtendere pakati pawo mwachilungamo. Ndithudi
Mulungu amakonda iwo amene amachita chilungamo.
10. Onse okhulupirira ali pachibale. Kotero khazikitsani
mtendere ndi kukhululukirana ndi abale anu ndipo opani
Mulungu kuti mulandire chisomo chake.

11. Oh inu anthu okhulupirira! Musalole kuti anthu ena
aziseka anzawo. Mwina kungatheke kuti gulu limene
lisekedwa likhoza kukhala labwino kuposa limene likuseka.
Ndiponso musalole akazi kuti aseke anzawo chifukwa
mwina kungatheke kuti osekedwawo akhoza kukhala
abwino kuposa osekawo. Musafunirane zifukwa wina
ndi mnzake kapena kuitanana ndi mayina a mchedzera.
Mayina a mchedzera ndi oipa kwa amene wakhulupirira.
Ndipo aliyense amene sasiya kuitana anzake ndi maina a
mchedzera , ameneyo ndiye wopanda chilungamo.

12. Oh inu anthu akhulupirira! Pewani kukaikirana
chifukwa kukhala ndi chikayiko ndi tchimo. Ndipo

musachite ukazitape pakati panu kapena amiseche. Kodi
wina wa inu angakondwere kudya mnofu wa mnzake amene
ndi wakufa? Kodi koma inu mumakana kudya.. Kotero
opani Mulungu. Ndithudi Mulungu amabwezera chisoni
chifukwa ndiye Mwini Chisoni Chosatha.
13. Oh anthu inu inu! Ndithudi Ife tidakulengani inu
mwamuna ndi mkazi ndipo tidakupangani inu kukhala
mitundu ya anthu ndi mabanja muzidziwana, Ndithudi
wopambana kwambiri pakati panu ndiponso pamaso pa
Mulungu ndi amene amaopa Mulungu. Ndithudi Mulungu
ndi wodziwa chinthu china chilichonse.
14. Anthu okhala m'midzi amati, "Ife timakhulupirira."
Nena, "Inu mulibe chikhulupiriro. Koma nenani kuti,
"Tadzipereka kwa Mulungu chifukwa chikhulupiriro
sichidakhazikike m'mitima mwanu. Ndipo ngati inu
mumvera Mulungu ndi Mtumwi wake, Iye sadzachepetsa
ntchito zanu, ngakhale m'pang'ono pomwe. Ndithudi
Mulungu ndi wokhululukira nthawi zonse ndi Mwini
chisoni chosatha." 15. Okhulupirira ndi okhawo amene
amakhulupirira mwa Mulungu ndi Mtumwi wake ndipo
sakayika ngakhale ndi pang'ono pomwe. Iwo amadzipereka
kwathunthu pamodzi ndi chuma chawo m'njira ya
Mulungu. Ndipo iwo ndiwo olungama.
16. Nena, "Kodi inu mungamuphunzitse Mulungu
za chipembedzo chanu? Pamene Mulungu amadziwa
chilichonse chili mlengalenga ndi padziko lapansi. Ndipo
Mulungundi wodziwa chilichonse. 17. Iwo amaganiza kuti
ali kukuchitira iwe chisoni pamene alowa Chisilamu.
Nena, "Inu simuli kundichitira ine chisoni polowa
chisilamu. Iyayi, koma ndi Mulungu amene wakuchitirani

inu chisoni pokulangizani njira yoyenera ngati inu, muli
anthu olungama.” 18. Ndithudi Mulungu amadziwa zobisika
zonse zimene zili mlengalenga ndi padziko lapansi ndipo
Mulungu amaona zonse zimene mumachita.

Sura 50 • ‘Kâf

# Qaf

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. *Qaf*.

Pali Buku lolemekezeka la Korani. 2. Koma iwo alikudabwa
kuti kwa iwo kwadza mchenjezi wochokera pakati pawo.
Motero anthu osakhulupirira amati, “chimenechi ndi
chinthu chachilendo!” 3. “Pamene ife tafa ndi kusanduka
dothi, kubwerera kotero ndi kosatheka.” 4. Ife timadziwa
onse amene adamezedwa ndi nthaka ndipo Ife tili ndi Buku
la mbiri yawo. 5. Iyayi, koma iwo adakana choonadi pamene
chidadza kwa iwo. Kotero iwo, tsopano, asokonezeka.
6. Kodi iwo sayang’ana kumwamba ndi kuona mmene
tidakukonzera ndi kukukongoletsera ndi kuona kuti kulibe
mipata? 7. Ndipo dziko lapansi Ife talipanga kukhala losalala
ndi kuikamo mapiri ndipo tidameretsa mu dzikolo mbewu
zokongola zosiyanasiyana. 8. Choonetsa ndi chikumbutso
kwa kapolo aliyense amene amatembenukira nthawi
zonse kwa Mulungu. 9. Ndipo timatumiza kuchokera ku
mitambo mvula yodalitsika ndipo timameretsa m’minda
mbewu zimene zimakololedwa. 10. Ndi mitengo italiitali

ya tende yolemedwa ndi zipatso. 11. Chakudya cha akapolo.
Ndipo Ife timapereka moyo kunthaka imene idali yakufa.
Kumeneko ndiko kuuka kwa akufa.
12. Adakana iwo asanadze, anthu a Nowa ndi iwo amene
anali kukhala ku Ar-Rass ndi Thamoud. 13. Anthu a mtundu
wa Aad ndi Farawo ndi abale ake a Loti. 14. Ndi iwo
amene anali kukhala m’nkhalango ndi anthu a ku Tuba,
aliyense wa iwo adakana Atumwi ndipo chenjezo langa
lidakwaniritsidwa. 15. Kodi Ife tidatopa ndi chilengedwe
choyamba? Iyayi. Iwo asokonezeka ndi nkhani zokhudza
chilengedwe chatsopano.
16. Ndithudi Ife tidamulenga munthu ndipo timadziwa
zimene mtima wake umamuuza. Ndipo Ife tili pafupi ndi
iye kuposa mtsempha wa moyo wake. 17. Pamene asungi
awiri amulandira, wina atakhala kudzanja lamanja ndi wina
ku dzanja lamanzere. 18. Palibe mawu amene amayankhula
amene samveka kwa Msungi wa tcheru.
19. Ndipo ululu wa imfa udzadza pa iye mwachoonadi.
Ichi ndicho chimene iwe unali kuyesetsa kuchithawa.
20. Ndipo lipenga lidzaombedwa ndipo limeneli lidzakhala
tsiku loopseza. 21. Ndipo mzimu uliwonse udzadza pamodzi
ndi mngelo wouyendetsa ndi mngelo wochitira umboni.
22. (Ndipo kudzanenedwa kwa anthu ochimwa) kuti,
“Ndithudi inu simudafune kuchenjezedwa za chimenechi
ndipo tsopano Ife tavundukula chimene chimakuphimbani.
Ndipo lero maso anu ali kuona zenizeni.” 23. Ndipo mnzake
adzati, “Uwu ndi umboni umene ndili nawo.” 24. “Ponyani
ku Gahena aliyense wosathokoza ndiponso wosamvera.”
25. “Woletsa kuchita ntchito zabwino, woswa malamulo
ndiponso wokayika.” 26. “Iye amene anali kukhazikitsa

milungu ina yoonjezera pa Mulungu weniweni, motero
mponyeni ku chilango chowawa.” 27. Mnzake adzanena kuti,
“Ambuye wathu! Ine sindidamuuze kuti aziswa malamulo
ayi koma iye adadzisocheretsa yekha.” 28. Mulungu adzati,
“Musakangane pamaso panga. Ine ndidakutumizirani
chenjezo lokwanira.” 29. Chilango sichisintha ayi ndipo Ine
sindionetsa chinyengo kwa akapolo anga.
30. Patsiku limene Ife tidzaifunsa Gahena kuti, “Kodi
mwadzadza?” Ndipo iyo idzati, “Kodi akanalipobe ena?”
31. Ndipo Paradiso idzabweretsedwa kufupi kwa anthu
olungama. 32. Ichi ndicho chimene mudalonjezedwa ndipo
ndi mphotho kwa iye amene amadzipereka kwa Mulungu
nthawi zonse nasunga malamulo ake. 33. Ndiponso kwa iye
amene amaopa Mwini chisoni chosatha wosaoneka ndipo
amadza kwa Iye ndi mtima wodzichepetsa. 34. Lowani
m’menemo mwamtendere ndi mosaopa ayi. Ili ndi tsiku
la moyo wosatha. 35. M’menemo mudzakhala chilichonse
chimene iwo adzafuna ndipo Ife tili ndi zinthu zambiri.
36. Kodi ndi mibadwo ingati imene Ife tidaiononga iwo
asanabadwe amene adali ndi mphamvu zoposa iwo ndipo
iwo adafuna chitetezo padziko? Kodi iwo anali ndi kwina
kothawira? 37. Ndithudi muli chikumbutso mu zimenezi
kwa iye amene ali ndi mtima kapena amatchera khutu
pamene achenjezedwa.
38. Ndithudi Ife tidalenga kumwamba ndi dziko lapansi
ndi zonse zimene zili m’menemo m’masiku asanu ndi
limodzi ndipo sitidatope ayi. 39. Kotero pirira pa zonse
zimene amanena ndipo lemekeza Ambuye wako dzuwa
lisanatuluke ndiponso lisanalowe. 40. Ndipo mulemekeze
Iye usiku ndipo utatha kupemphera.

41. Ndipo udzamve patsiku limene woitana adzaitana
kuchokera pafupi. 42. Tsiku limene iwo adzamva kulira kwa
mfuwu woona. Limeneli lidzakhala tsiku louka kwa akufa.
43. Ndithudi ndife amene timapereka moyo ndi imfa ndipo
ndi kwa Ife kumene zonse zidzabwerera. 44. Tsiku limene
dziko lidzang'ambika ndipo iwo adzatuluka mofulumira.
Kumeneko ndiko kudzakhala kusonkhanitsidwa pamodzi.
45. Ife timadziwa zonse zimene amanena ndipo iwe si
ndiwe wankhanza ayi. Koma muchenjeze ndi Korani kwa
aliyense amene aopa chilango changa.

SURA 51 • AD-DHÂRIYÂT

# ZARIAT

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pali mphepo imene imamwaza fumbi. 2. Ndi mitambo
imene ili yolemedwa ndi madzi. 3. Ndi zombo zimene
zimayenda mosavutika ndi mwabata. 4. Ndipo pali
iwo amene amagawa madalitso ndi chilolezo chathu.
5. Ndithudi chimene mwalonjezedwa, ndithudi, ndi
choona. 6. Ndithudi chiweruzo chidzakwaniritsidwa. 7.
Pali kumwamba kumene kuli njira zambiri. 8. Ndithudi inu
muli ndi maganizo osiyana. 9. Amene abwezedwa ku icho
ndiye amene wabwezedwa. 10. Wotembereredwa akhale
amene amanama. 11. Amene akutidwa ndi kusamvera 12.
Iwo amafunsa kuti, "Kodi tsiku lachiweruzo lidzadza liti?"
13. Tsiku limene iwo adzaweruzidwa ndi kuponyedwa ku

moto. 14. Lawani chilango chanu! Ichi ndicho chimene
munali kufuna kuti chidze msanga. 15. Ndithudi iwo amene
amalewa machimo adzakhala m'minda imene ili ndi a
kasupe. 16. Kulandira zimene Ambuye wawo awapatsa.
Ndithudi kale iwo anali kuchita zinthu zabwino. 17. Iwo anali
kugona nthawi yochepa usiku. 18. Ndipo m'bandakucha
anali kupempha chikhululukiro. 19. Ndipo mu chuma
chawo mudali gawo limene linali kuperekedwa kwa anthu
opempha ndi osowa.

20. Ndipo m'dziko muli zizindikiro kwa iwo okhulupirira.
21. Ndi mizimu yanu kodi simungaone? 22. Ndipo kumwamba
ndiko kuli chakudya chanu ndi zimene muli kulonjezedwa.
23. Ndiye, pali Ambuye wakumwamba ndi dziko lapansi,
chimenechi ndi cholinga ndi choonadi chomwe inu
mumayankhula.

24. Kodi udamva nkhani ya alendo olemekezeka a
Abrahamu? 25. Pamene iwo adadza kwa iye, iwo adati,
"Mtendere." Ndipo iye adati, "Mtendere." Ndipo iye adati,
"Inu ndinu alendo kwa ine." 26. Ndipo iye atapita ku banja
lake adabweretsa nyama ya ng'ombe yowotcha. 27. Motero
iye adadza nayo kwa iwo nati, "Kodi simufuna kudya?"
28. Motero iye adayamba kuchita mantha mu mtima
mwake. Ndipo iwo adati, "Usaope." Ndipo iwo adamuuza
nkhani yabwino yakubadwa kwa mwana wamwamuna
yemwe adzakhala wanzeru kwambiri. 29. Ndipo mkazi
wake adadza modzichepetsa ndipo adamenya pa mphumi
pake nati, "Nkhalamba yaikazi yosaberekapo!" 30. Iwo
adati, "Ngakhale ndi choncho, Ambuye wako wayankhula.
Iye ndi wodzala ndi luntha ndiponso nzeru."

31. Iye adati, "Kodi inu Atumwi uthenga wanu ndi wotani?"

32. Iwo adati, "Ife tatumidwa kwa anthu ochimwa." 33. "Kuti
tigwetse pa iwo miyala yamakande." 34. "Idakonzedwa ndi
Ambuye wako kudza kwa anthu oswa malamulo." 35. Ndipo
Ife tidatulutsa anthu okhulupirira amene adali momwemo.
36. Koma sitidapezemo mabanja a Chisilamu kupatula banja
limodzi lokha basi. 37. Ndipo Ife tidasiyamo chizindikiro
kwa iwo amene amaopa chilango chowawa.

38. Ndi mwa Mose. Pamene tidamutumiza kwa Farawo
ndi zizindikiro zooneka. 39. Koma Farawo adakana pamodzi
ndi mafumu ake nati, "Ndiwe munthu wamatsenga kapena
munthu wa misala." 40. Motero tidamugwira pamodzi
ndi gulu la asirikali ake ndi kuwamiza onse m'nyanja
pamene iye ndiye adali wolakwa. 41. Ndipo mwa a Aad
pamene tidawatumizira mphepo yoononga. 42. Imene
sidasiye chilichonse chimene idalimbana nacho kupatula
kuchiononga ndi kuchisandutsa phulusa. 43. Ndipo mwa
anthu a Thamoud. Pamene adauzidwa kuti, "Basangalalani
kanthawi kochepa." 44. Koma iwo adaphwanya lamulo la
Ambuye wawo mwamwano, kotero mabingu adawaononga
iwo ali kuona. 45. Kotero iwo adalibe mphamvu zodzuka
kapena zodzitetezera. 46. Ndi anthu a Nowa iwo asanadze.
Ndithudi iwo adali anthu oswa malamulo.

47. Ife tidakonza kumwamba mwamphamvu ndiponso
mwaluso. Ndipo, ndithudi, ndife amene timapanga kukula
kwa mlengalenga. 48. Ndipo dziko, tidamwaza. Kodi ndife
omwaza bwino bwanji! 49. Ndipo zonse zimene tidalenga
tidazilenga ziwiriziwiri kuti mukhoza kukumbukira.
50. Kotero thawirani kwa Mulungu. Ndithudi Ine ndine
mchenjezi wooneka kwa inu wochokera kwa Iye. 51. Ndipo
musapange fano kukhala lopembedzedwa pamodzi ndi

Mulungu. Ndithudi ine ndine mchenjezi wooneka kwa inu
wochokera kwa Iye.
52. Chimodzimodzi palibe Mtumwi amene adadza kwa
anthu amene sadamunenere mawu ofanana monga akuti:
"Wamatsenga kapena munthu wopenga!" 53. Kodi uwu ndi
mwambo umene akhala ali kusiyirana wina ndi mnzake?
Iyayi, iwo ndi anthu amene ali kuswa malamulo mopyola
muyeso. 54. Kotero uwaleke chifukwa iwe ulibe mlandu.
55. Ndipo kumbutsa chifukwa chikumbutso chimathandiza
anthu okhulupirira.
56. Ndipo Ine ndidalenga majini ndi anthu kuti
azindipembedza Ine. 57. Ine sindiwapempha chakudya
ndipo sindiwafunsa kuti azindidyetsa Ine. 58. Ndithudi
ndi Mulungu yekha amene amapereka chakudya chonse,
Mwini mphamvu zonse ndi wolimba kwambiri. 59. Ndithudi
anthu onse olakwa adzalandira gawo longa limene anzawo
olakwa akale adalandira, kotero asandifunse Ine kuchita
mofulumira. 60. Kotero tsoka kwa onse osakhulupirira
kuchokera ku tsiku lomwe iwo alonjezedwa.

Sura 52 • At-Tûr

# Al Tur

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ndi pali phiri! 2. Ndi pali Buku lolemekezeka. 3. Lili
chikopa chosapinda. 4. Ndi pali Bait – Ul-Ma'mur (Nyumba
imene ili kumwamba yolingana ndi Kaaba imene ili ku

Makka ndipo imaonedwa ndi angelo pafupipafupi). 5. Ndi
pali denga lonyamuka. 6. Ndi pali nyanja yodzadzidwa
ndi madzi ambiri. 7. Ndithudi chilango cha Ambuye wako
chidzakwaniritsidwa. 8. Palibe wina amene angachiletse.
9. Pa tsiku limeneli, kumwamba kudzagwedezeka koopsa.
10. Ndipo mapiri adzagudubuzika osakhalanso china
chake. 11. Kotero tsoka, patsiku limeneli kwa anthu abodza.
12. Amene amatangwanika ndi mabodza. 13. Patsikuli iwo
adzatengedwa ndi kuponyedwa mwamphamvu ku moto
wa ku Gahena. 14. Uwu ndi moto umene mumati ndi bodza.
15. Kodi amenewa ndi matsenga kapena simutha kuona?
16. Lawani kutentha kwake ndipo kaya inu mupirira kapena
ayi, kwa inu ndi chimodzimodzi; inu muli kulandira
malipiro a ntchito zomwe mumachita.

17. Ndithudi iwo amene ali olungama, adzakhala
m'minda mwamtendere. 18. Kusangalala chifukwa cha
zimene Ambuye wawo wawapatsa ndipo Ambuye wawo
wawapulumutsa ku chilango cha ku Gahena. 19. "Idyani
ndi kumwa mwachisangalalo chifukwa cha ntchito
zanu zabwino zomwe mudachita." 20. Iwo adzakhala pa
mipando yawofowofo, yoikidwa m'mizere. Ndipo Ife
tidzawakwatitsa kwa amene ali ndi maso akuluakulu ndi
okongola.

21. Ndipo iwo amene amakhulupirira ndipo ana awo
amawatsatira m'chipembedzo, oterewa tidzawakumaniza
ndi mabanja awo ndipo Ife sitidzawachotsera chilichonse
cha malipiro a ntchito zawo zabwino. Munthu aliyense
adzafunsidwa malinga ndi ntchito zake. 22. Ndipo
tidzawapatsa zipatso ndi nyama zimene iwo afuna.
23. Kumeneko iwo adzapatsana wina ndi mnzake chikho

chimene mulibe zinthu zopanda pake kapena uchimo.
24. Iwo adzazunguliridwa ndi kutchingidwa bwino ndi
anyamata awoawo amene adzawatumizira ngati kuti iwo
anali ndolo zobisika. 25. Ndipo iwo adzafunsana wina ndi
mnzake ndi kuyankhulitsana. 26. Iwo adzati, "Kale ife
tidali a mantha ndi mabanja athu." 27. "Koma Mulungu
wationetsera chisomo chake ndipo watipulumutsa ife ku
chilango cha kumoto." 28. "Ndithudi ife tinali kumupempha
Iye yekha. Ndithudi Iye ndiye Mwini chifundo ndi Mwini
chisoni chosatha."
29. Motero pitiriza kukumbutsa ndi kulalikira. Chifukwa
cha chisomo cha Ambuye wako, iwe si ndiwe munthu
wonyenga kapena wamisala. 30. Kapena iwo amati, "Ndi
Mlakatuli, ife tili kuyembekezera kuti choipa chidze pa
iye." 31. Nena, "Yembekezerani! Nanenso ndili mmodzi
wa oyembekezera." 32. Kodi ndi maganizo awo amene
ali kumawauza izi kapena iwo ndi anthu amene amaswa
malamulo mosadodoma? 33. Kodi kapena iwo amati, "Iye
wapeka yekha uthengawu? Iyayi! iwo alibe chikhulupiriro."
34. Alekeni nawo abweretse mawu olingana ndi awa ngati
iwo ali kunena zoona.
35. Kodi iwo adalengedwa popanda china chake kapena
iwo ndiwo a Namalenga? 36. Kapena ndiwo amene
adalenga kumwamba ndi dziko lapansi? Iyayi! iwo alibe
chikhulupiriro chokhazikika. 37. Kodi ndiwo amene
amasunga chuma cha Ambuye wako? Kapena iwo ndiwo
a nkhanza amene ali ndi ulamuliro wonena chilichonse
chimene afuna? 38. Kodi kapena iwo ali ndi njira yomvetsera
zomwe zinali kunenedwa? Motero mulekeni kazitape

wawo kuti apereke umboni wokwanira. 39. Kodi kapena Iye
ali ndi ana aakazi okha pamene inuyo muli ndi ana aamuna?
40. Kodi kapena iwe uli kuwafunsa malipiro kotero kuti
iwo apanikizidwa kwambiri ndi ngongole? 41. Kodi kapena
ali ndi zobisika ndipo amazilemba? 42. Kodi kapena ali
kukonza chiwembu? Koma iwo amene sakhulupirira ndiwo
amene ali ndi chiwembu! 43. Kodi kapena ali ndi mulungu
wina kupatula Mulungu weniweni? Mulungu alemekezeke
kuposa zimene iwo amamufanizira nazo.
44. Ndipo iwo akadaona gawo lina la kumwamba lili
kugwa pansi ndipo iwo akadati, "Ndi mitambo youndana."
45. Motero alekeni mpaka pamene iwo akumana ndi
tsiku lawo limene iwo adzakomoka ndi mantha. 46. Tsiku
limene chiwembu sichidzawathandiza china chilichonse
ndipo chithandizo sichidzaperekedwa kwa iwo. 47. Ndipo,
ndithudi, onse amene amachita zoipa, kuli chilango china
pa chilango ichi koma ambiri a iwo sadziwa.
48. Motero pirira podikira chiweruzo cha Ambuye wako,
chifukwa ndithudi iwe uli kusamalidwa ndi Ife ndipo
lemekeza Ambuye wako pamene uuka ku tulo. 49. Nthawi
ya usiku, lemekeza ulemerero wake ndi pa nthawi yolowa
nyenyezi.

# AL NAJM

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ndi pali nyenyezi pamene ili kulowa. 2. M'bale wanu
sadasochere kapena kuti ndi wolakwa. 3. Ndipo iye
sayankhula zofuna zake. 4. Icho ndi chochita kuuzidwa kwa
iye. 5. Iye adaphunzitsidwa ndi Iye amene ali ndi mphamvu.
6. Wopanda chilema chilichonse, kotero adadzuka ndi
kukhala wokhazikika. 7. Pamene iye anali patali kwambiri
mu mlengalenga. 8. Ndipo adasendera ndi kudza pafupi.
9. Ndipo adali pa mtunda wolingana kuponya mipaliro iwiri
kapena kucheperapo. 10. Motero Iye adaulula Uthenga kwa
kapolo wake kudzera mwa Gabriyele. 11. Mtima wake wa
Mtumwi siudaname ponena zimene iye adaona. 12. Kodi
inu mudzatsutsana naye pa zimene iye adaona? 13. Ndithudi
iye adamuona iye pamene anali kutsika kachiwiri. 14. Pafupi
ndi mtengo wa Sidrah. 15. Pafupi pake pali munda womwe
ndi malo opumirako. 16. Ndipo chimene chimaphimba
chidakuta mtengo wa Sidrah. 17. Maso ake sadayang'ane
kumbali kapena kupyola muyeso. 18. Ndithudi iye adaona
zizindikiro zazikulu kwambiri za Ambuye wake.

19. Kodi inu maganiza za Lat ndi Uzza? 20. Ndi Manat
wachitatu wamkazi? 21. Kwa inu amuna ndipo kwa Iye akazi?
22. Ndithudi kumeneku ndiko kugawa kosalungama! 23. Awa
ndi mayina chabe amene inu mwapeka, inu ndi atate anu,
amene Mulungu sadakulamuleni ndi pang'ono pomwe. Iwo

amangotsatira nkhani zakumva chabe zimene mitima yawo
imafuna pamene, ndithudi, kwadza kale kwa iwo ulangizi
wochokera kwa Ambuye wawo. 24. Kodi munthu angapeze
zonse zimene amafuna? 25. Koma Mulungu ndiye Mwini
moyo umene uli nkudza ndi moyo wakale.

26. Ndipo kuli angelo ambiri amene ali kumwamba
amene kukhala pakati kwawo sikudzathandiza chilichonse
kupatula pokhapo pamene Mulungu apereka chilolezo
kwa amene Iye wamufuna ndi kukondweretsedwa
naye. 27. Ndithudi iwo amene sakhulupirira za m'moyo
umene uli nkudza, amatcha angelo ndi mayina achikazi.
28. Pamene iwo sadziwa chilichonse cha izo. Iwo satsatira
china chilichonse koma nkhani zabodza ndipo, ndithudi,
nkhani zabodza si mlowam'malo wa choonadi. 29. Motero
mupewe wina aliyense amene salabadira chikumbutso
chathu ndipo safuna china chilichonse koma moyo wa
padziko lino lapansi. 30. Uko ndiko kuchuluka kwa nzeru
zawo. Ndithudi Ambuye wako ndiye amadziwa bwino
onse amene amasochera ku njira yoyenera ndipo amadziwa
kwambiri iye amene amatsata njira yoyenera.

31. Ndipo Mulungu ndiye mwini wake wa chilichonse
chimene chili kumwamba ndi dziko lapansi, ndipo akhoza
kulanga onse amene amachita zoipa molingana ndi ntchito
zawo ndiponso kuti akhoza kulipira onse amene amachita
zabwino ndi mphotho yabwino kwambiri. 32. Iwo amene
amapewa machimo a akuluakulu ndi chigololo kupatula
machimo a ang'onoang'ono, ndithudi, Ambuye wako ndi
Mwini chikhululukiro. Iye amakudziwani bwino pamene
amakulengani kuchokera ku dothi ndi pamene mukutidwa
m'mimba mwa amayi anu. Motero musadziyeretse nokha.

Iye amadziwa bwino kwambiri aliyense amene amalewa
zoipa.
33. Kodi iwe wamuona amene amabwerera m'mbuyo?
34. Amene adapereka pang'ono ndipo anasiya kupereka?
35. Kodi iye amadziwa za zinthu zobisika kuti akhoza
kuziona? 36. Kodi kapena iye sadauzidwe za mawu amene
ali m'mabuku a Mose? 37. Ndiponso za Abrahamu amene
adakwaniritsa malamulo? 38. Kuti palibe munthu amene
adzasenza katundu wa mnzake. 39. Ndipo kuti munthu
sadzapeza chilichonse kupatula chimene wachigwirira
ntchito. 40. Ndipo kuti ntchito zake zidzaoneka.
41. Pamenepo iye adzalipidwa malipiro ake oyenera.
42. Ndipo kuti kwa Ambuye wanu ndi kumene nonse
mudzapita. 43. Ndipo kuti Ndiye amene amawachititsa
anthu kuseka ndi kuwaliritsa. 44. Ndipo kuti Ndiye
amene amapereka imfa ndi moyo. 45. Ndiponso kuti Iye
adalenga zinthu ziwiriziwiri, chachimuna ndi chachikazi.
46. Kuchokera ku madontho a umuna umene umatuluka.
47. Ndipo kuti kwa Iye kuli chilengedwe chachiwiri.
48. Ndipo kuti Ndiye amene amapereka chuma ndi
chisangalalo. 49. Ndipo kuti Iye ndiye Ambuye wa nyenyezi
yamphamvu yotchedwa Sirius.
50. Kuti ndiye amene adaononga anthu akale a mphamvu
kwambiri a mtundu wa a Aad kale. 51. Ndi anthu a mtundu
wa a Thamoud. Ndipo Iye sadasiye wina aliyense. 52. Ndi
anthu a Nowa amakedzana ndithudi iwo adali osalungama
ndi oswa malamulo mwamwano. 53. Ndipo iye adaononga
mizinda yomwe idali yogonjetsedwa. 54. Kotero iwo
adawavundikira nd chimene chidawavundikira. 55. Kodi
ndi zokoma ziti za Ambuye wako zimene udzazikayikira?

56. Uyu ndi mchenjezi wotsatizana ndi achenjezi a
makedzana. 57. Tsiku louka kwa akufa lili pafupi. 58. Palibe
wina kupatula Mulungu amene akhoza kulipherera.
59. Kodi inu mulikudabwa pa zimene zili kulakatulidwa?
60. Ndipo inu muli kuseka m’malo mwakulira? 61. Ndi
kumapitirizabe kuchita zinthu zopanda pake? 62. Motero
gunditsani nkhope zanu pansi ndipo pembedzani Mulungu
mmodzi yekha.

Sura 54 • Al-’Kamar

# Qamar

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ola lachiweruzo lili pafupi ndipo mwezi wagawanika
pakati. 2. Koma iwo akaona chozizwitsa, sakhulupirira
ndipo amati, “Ichi sichina ayi koma matsenga ozama.”
3. Iwo amakana choonadi koma amatsatira zilakolako
zawo. Koma chinthu chilichonse chili ndi kumaliza kwake.
4. Ndithudi uthenga waperekedwa kale kwa iwo umene uli
ndi chenjezo. 5. Wodzadzidwa ndi nzeru koma machenjezo
ake sawathandiza iwo china chilichonse. 6. Kotero iwe,
asiye okha. Patsiku limene woitana adzawaitana kudza
ku chinthu choopsa 7. Iwo adzadza kumeneko ndi nkhope
zogwa pansi, kuchokera kumanda awo monga dzombe
louluka ponseponse. 8. Adzadza mofulumira kwa oitana
anthu osakhulupirira adzati, “Ili ndi tsiku lovuta kwambiri.”
9. Asanadze iwo, anthu a Nowa adakana kapolo wathu

ndipo adati, “Uyu ndi munthu wamisala.” Ndipo iwo
adamuthamangitsa iye ndi kumunyoza kwambiri. 10. Ndipo
iye adadandaula kwa Ambuye wake nati, “Ndagonjetsedwa
kotero idzani kuti mundithandize.” 11. Motero Ife
tidatsekula makomo a kumwamba, ndipo mvula idagwa
nthawi yomweyo. 12. Ndipo tidatumphutsa a kasupe
padziko lapansi kotero madzi onse adakumana monga
mwa lamulo lathu. 13. Ndipo tidamunyamula iye m’chombo
chopangidwa ndi matabwa ndi chokhomedwa ndi misomali.
14. Chidanyamuka potsogozedwa ndi Ife. Mphotho kwa
iye amene adakanidwa! 15. Ndithudi tidachisiya icho ngati
chizindikiro koma kodi alipo ena amene adzachenjezedwa?
16. Kodi chilango changa ndi chenjezo langa zidali zalikulu
bwanji? 17. Ndithudi talipanga Buku la Korani kukhala
losavuta kulidziwa ndi kulikumbukira. Kodi alipo ena
amene adzachenjezedwa?
18. Anthu a Aad adakana. Kodi chilango changa ndi
chenjezo langa zidali zoopsa bwanji? 19. Ndithudi Ife
tidatumiza mphepo yamkhuntho pa tsiku latsoka
losasimbika. 20. Kugwetsa anthu ngati kuti adali mathunthu
a mitengo ya mgwalangwa yozulidwa. 21. Kodi chilango
changa ndipo chenjezo langa zidali zoopsa bwanji?
22. Ndithudi talipanga Buku la Korani kukhala losavuta
kulizindikira ndi kulikumbukira. Kodi alipo ena amene
adzachenjezedwa?
23. Anthu a Thamoud adakana machenjezo. 24. Iwo
adati, “Munthu! Mmodzi yekha wochokera ku mtundu
wathu kuti timutsatire? Ndithudi ife tikhala olakwa
kwambiri ndiponso a misala.” 25. “Kodi ndiye kuti uthenga
waperekedwa kwa iye yekha pakati pa ife tonse? Iyayi! Iye

ndi wabodza ndi wodzikweza.” 26. Mawa iwo adzadziwa
kuti wabodza ndi wodzikweza ndani. 27. Ndithudi Ife
titumiza ngamira yaikazi ngati mayesero kwa iwo. Motero
iwe uwapenyetsetse ndipo ukhale wopirira. 28. Ndipo
uwauze kuti azigawana madzi. Ndipo nthawi yomwera
madzi idzakhazikitsidwa. 29. Ndipo iwo adaitana m’bale
wawo ndipo iye adatulutsa lupanga ndi kuipha. 30. Kodi
chilango changa ndi chenjezo langa zidali zoopsa bwanji?
31. Ndithudi tidawatumizira mfuwu umodzi ndipo onse
adali ngati nkhuni zodula zimene munthu womanga
mpanda amatola. 32. Ndithudi talipanga Buku la Korani
kukhala losavuta kulizindikira ndi kulikumbukira. Koma
kodi alipo ena amene adzachenjezedwa?

33. Anthu a Loti adati chenjezo lathu ndi labodza.
34. Ndithudi Ife tidawatumizira mphepo yonyamula miyala
kupatula a pa banja la Loti amene tidawapulumutsa mu
ola lomaliza la usiku. 35. Monga chisomo chochokera
kwa Ife, motero ndi mmene timalipirira anthu oyamika.
36. Ndithudi iye adawachenjeza za chilango chathu choopsa
koma iwo adakana chenjezo lathu. 37. Ndipo, ndithudi,
iwo adafuna kuchititsa manyazi alendo ake. Motero Ife
tidawachititsa khungu. Kotero inu lawani chilango changa
ndi machenjezo anga. 38. Ndithudi chilango chowawa
chidadza pa iwo nthawi yam’mawa. 39. Kotero inu lawani
chilango changa ndi machenjezo anga. 40. Ndithudi
talipanga Buku la Korani kukhala losavuta kulizindikira ndi
kulikumbukira. Kodi alipo ena amene adzachenjezedwa?

41. Ndipo, ndithudi, machenjezo adadza kwa anthu a
Farawo. 42. Iwo adati machenjezo athu onse ndi abodza

motero tidawaononga ndi chilango champhamvu
yochuluka.
43. Kodi anthu anu osakhulupirira ndi abwino kuposa
awa? Kapena inu muli ndi chitetezo mu m'mawu a
Mulungu? 44. Kodi kapena iwo amati, "Ife ndife ambiri
ndipo tidzapambana?" 45. Tsopano magulu awo ali
kupirikitsidwa ndipo iwo ali kuthawa. 46. Iyayi, koma ola
lachiweruzo ndi nthawi imene iwo adalonjezedwa ndipo
ola limeneli lidzakhala loopsa kwambiri. 47. Ndithudi
anthu osakhulupirira ndi olakwa adzapsya. 48. Tsiku limene
iwo adzaduduluzidwa pa nkhope zawo kunka ku moto,
(zidzanenedwa) "Lawani ululu wa ku Moto."
49. Ndithudi tidalenga chilichonse molingana ndi muyeso
wake. 50. Ndipo ulamuliro wathu ndi umodzi monga
kuphenira kwa diso. 51. Ndithudi Ife tidaononga kale
anthu onga inu koma kodi alipo amene anga chenjezedwe?
52. Ndipo zonse zimene adachita zidalembedwa. 53. Ndipo
chilichonse chaching'ono ndi chachikulu chidalembedwa
kale. 54. Ndithudi onse amene amalewa zoipa adzakhala
m'kati mwa minda ndi mitsinje. 55. Ku Paradiso kufupi ndi
Mfumu yamphamvu zonse.

# RAHMAN

M'dzina la Mulungu Mwini, Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Mwini Chifundo Chosatha. 2. Ndiye amene
adamphunzitsa munthu Korani. 3. Ndiye amene adalenga
munthu. 4. Wamuphunzitsa iye mawu anzeru. 5. Dzuwa
ndi mwezi zimayenda m'misewu imene zinalamulidwa.
6. Zomera (kapena nyenyezi) ndi mitengo zonse zimagwada
pomulambira Iye. 7. Iye adakweza kumwamba ndi
kukhazikitsa muyeso. 8. Kuti inu musaphwanye muyeso.
9. Kotero khazikitsani muyeso wachilungamo ndipo
musayese monyenga.
10. Ndiye amene adalenga dziko lapansi kuti zolengedwa
zake zizikhalamo. 11. Mu ilo muli zipatso ndi mitengo
ya tende yobereka phava la zipatso zambiri. 12. Ndi
chimanga chimene masamba ndi mapesi ake amadyedwa
ndi ziweto. Ndi mitengo yonunkhira. 13. Kodi ndi zokoma
ziti za Ambuye wanu zimene mudzakana? 14. Iye adalenga
munthu kuchokera ku dothi monga dothi la mbiya.
15. Ndipo adalenga majini kuchokera kumoto wopanda
utsi. 16. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene
mudzakana? 17. Ambuye wa kum'mawa kuwiri ndi Ambuye
wa kumadzulo kuwiri. 18. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye
wanu zimene mudzakana? 19. Iye adasiya nyanja ziwiri kuti
zikumane. 20. Pakati pawo pali malire amene madzi a uku
sangathe kudutsa kupita uko. 21. Kodi ndi zokoma ziti za

Ambuye wanu zimene mudzakana? 22. Mu zonse muli
nkhombe zazikulu ndi zazing'ono. 23. Kodi ndi zokoma
ziti za Ambuye wanu zimene mudzakana? 24. Ndipo zake
ndi zombo zimene zimayenda pa nyanja, zazikulu ngati
mapiri. 25. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene
mudzakana?
26. Zonse zimene zili pa dziko zidzatha. 27. Ndipo
nkhope ya Ambuye wako mu Ufumu ndi mu Ulemerero
idzakhalabe mpaka kalekale. 28. Kodi ndi zokoma ziti
za Ambuye wanu zimene mudzakana? 29. Zonse zimene
zimakhala kumwamba ndi padziko lapansi zimapempha
kwa Iye. Tsiku lililonse Iye amakhala ndi chochita. 30. Kodi
ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene mudzakana?
31. Ife tidzadza kwa inu, Oh inu magulu awiri! 32. Kodi
ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene mudzakana?
33. Oh inu gulu la Majini ndi Anthu! Ngati muli ndi
mphamvu zodutsa malire a kumwamba ndi dziko lapansi,
dutsani. Komatu inu simungadutse popanda chilolezo. 34.
Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene mudzakana?
35. Malawi a moto ndi utsi zidzaponyedwa kwa inu nonse
awiri ndipo simudzatha kudziteteza nokha. 36. Kodi ndi
zokoma ziti za Ambuye wanu zimene mudzakana?
37. Ndi pamene thambo lidzagawanika pakati ndikukhala
lofiira ngati mafuta osungunuka. 38. Kodi ndi zokoma ziti
za Ambuye wanu zimene mudzakana? 39. Motero patsiku
limeneli, sipadzakhala mafunso kuchokera kwa Munthu
kapena Majini okhudza machimo awo. 40. Kodi ndi zokoma
ziti za Ambuye wanu zimene mudzakana? 41. Ochimwa
adzadziwika ndi zizindikiro ndipo adzawagwira tsumba
ndi pamapazi pawo. 42. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye

wanu zimene mudzakana? 43. Iyi ndi Gahena imene anthu
ochimwa amati ndi bodza. 44. Iwo adzalowa m'kati mwake
ndi m'kati mwa madzi ogaduka. 45. Kodi ndi zokoma ziti za
Ambuye wanu zimene mudzakana?

46. Ndipo kwa iye amene aopa kuima pamaso pa Ambuye
wawo, kudzakhala minda iwiri. 47. Kodi ndi zokoma ziti
za Ambuye wanu zimene mudzakana? 48. Zokhala ndi
mphanda zotambasuka. 49. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye
wanu zimene mudzakana? 50. Monse mudzakhala a kasupe
awiri otumphuka. 51. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye
wanu zimene mudzakana? 52. M'menemu mudzakhala
zipatso ziwiriziwiri za mitundumitundu. 53. Kodi ndi
zokoma ziti za Ambuye wanu zimene mudzakana? 54. Iwo
adzagona pa makama amene nsalu yake ya m'kati idzakhala
yasilika ndipo zipatso za m'minda iwiriyi zidzakhala pafupi
pawo. 55. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene
mudzakana? 56. M'menemo mudzakhala wodzisunga ndi
ogwetsa nkhope zawo pansi amene Munthu kapena Majini
sadawakhudze. 57. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu
zimene mudzakana? 58. Olingana ndi miyala ya Rubiya ndi
ndolo. 59. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene
mudzakana? 60. Kodi dipo la ntchito yabwino lingakhale
lina loposa ubwino? 61. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye
wanu zimene mudzakana?

62. Ndipo poonjezera pa minda iwiri pali minda ina iwiri.
63. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene
mudzakana? 64. Yooneka mobiriwira 65. Kodi ndi zokoma
ziti za Ambuye wanu zimene mudzakana? 66. Monse
mudzakhala a kasupe awiri otulutsa madzi ochuluka
67. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene

mudzakana? 68. Monse mudzakhala zipatso, tende ndi
chimanga chachizungu. 69. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye
wanu zimene mudzakana? 70. Mmenemo mudzakhala
zinthu zokongola. 71. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu
zimene mudzakana? 72. Angwiro ndi okhala m'mahema.
73. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu zimene
mudzakana? 74. Amene Munthu kapena Majini
sadawakhudze. 75. Kodi ndi zokoma ziti za Ambuye wanu
zimene mudzakana? 76. Atakhala pa mipando yawofowofo,
yobiriwira ndi mabedi okongola. 77. Kodi ndi zokoma ziti za
Ambuye wanu zimene mudzakana? 78. Lidalitsike dzina la
Ambuye wako, Mwini ulemerero, chuma ndi ulemu.

SURA 56 • AL-WÂ'KI'A

# AL WAQIA

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pamene ola la chiweruzo lidza. 2. Ndipo palibe mzimu
umene udzakana kudza kwake. 3. Kutsitsa gulu lina
ndikukweza gulu linzake. 4. Pamene dziko lidzagwedezeka
ndi chigwedezo choopsya. 5. Ndi pamene mapiri
adzafumbutuka kukhala fumbi lokhalokha. 6. Motero
iwo adzakhala fumbi louluzika paliponse. 7. Ndipo inu
mudzagawidwa m'magulu atatu.
8. Iwo a ku dzanja la manja. Kodi a ku dzanja la manja
adzakhala ndani? 9. Iwo akudzanja la mazere. Kodi
akudzanja la mazere adzakhala ndani? 10. Ndipo gulu la iwo

amene adzakhala kutsogolo m'chikhulupiriro adzakhala
kutsogolo m'moyo umene uli nkudza. 11. Awa ndiwo amene
adzakhala kufupi ndi Mulungu. 12. M'minda ya Paradiso.
13. Gulu lalikulu lidzachokera ku mibadwo ya kale. 14. Ndi
gulu lochepa lidzachokera ku mibadwo ya m'mbuyo mwake.
15. Iwo adzakhala pa mipando yawofowofo yomatidwa
golide ndi miyala ya mtengo wapatali. 16. Atakhala pa
iyo ndi kumayang'anizana. 17. Iwo adzatumikiridwa ndi
anyamata a muyaya. 18. Ndi mabakuli, miphika ndi zikho za
vinyo wabwino. 19. Amene sadzawawitsa mitu yawo kapena
kuwatopetsa. 20. Ndi zipatso zimene adzasankhepo 21. Ndi
nyama ya nkhuku imene angafune. 22. Ndipo padzakhala
anzawo okongola, a maso akulu ndi ochititsa kaso.
23. Monga ndolo zosamalidwa bwino. 24. Malipiro a ntchito
zimene adachita kale. 25. Palibe nkhani zopanda pake
kapena zolaula zimene adzamva. 26. Kupatula mawu akuti
Mtendere, Mtendere.

27. Iwo a kudzanja lamanja, kodi akudzanja lamanja
adzakhala ndani? 28. Iwo adzakhala pakati pa m'mithunzi
ya mitengo ya Sidrah. 29. Ndi m'mapata a nthochi zokhala
ndi mikoko wina pamwamba pa unzake. 30. M'mithunzi
yotambasuka. 31. Pambali pa madzi osefukira. 32. Ndi
zipatso zochuluka. 33. Zimene nyengo yake sikutha ndipo
kuchuluka kwake kudzakhalabe. 34. Ndi pa mipando
yawofowofo yokwezedwa. 35. Ndithudi Ife tawalenga iwo
mu chilengedwe cha padera. 36. Ndi kuwapanga kukhala
a Namwali abwino. 37. A chikondi pa anzawo olingana
nawo zaka. 38. A iwo amene adzakhala kudzanja lamanja.
39. Gulu lochuluka lidzakhala lochokera ku mibadwo

yoyamba, yakale. 40. Gulu lochuluka lidzakhala lochokera
ku mibadwo ya pambuyo pake.

41. Gulu la anthu a kudzanja lamanzere. Kodi anthu a
kudzanja la manzere adzakhala otani? 42. M'katikati mwa
malawi a moto ndi m'madzi ogaduka. 43. Ndi m'mithunzi
ya utsi wakuda. 44. Yosazizira kapena yabwino. 45. Ndithudi
iwo kale adali kukhala m'moyo wosavutika ndi opeza
zinthu zambiri. 46. Ndipo adapitirira kuchita zoipa
zikulu zikulu. 47. Ndipo iwo anali kukonda kunena kuti:
"Pamene ife tafa ndi kusanduka fumbi ndi mafupa, kodi
tingadzaukitsidwenso?" 48. "Ndi makolo athu a nthawi
ya makedzana?" 49. Nena: "Ndithudi onse oyambirira ndi
otsiriza." 50. "Ndithudi onse adzasonkhanitsidwa pamodzi
pa tsiku lokhazikitsidwa." 51. "Kuphatikiza inu nonse
amene muchimwa ndi kukana choonadi." 52. "Ndithudi
inu mudzadya zipatso za mtengo wa Zaqqoom." 53. "Ndipo
mudzakhutitsa mimba zanu ndi izo." 54. "Ndi kumwa madzi
ogaduka." 55. "Ndi kumwa monga momwe ngamira yodwala
ndi yaludzu imamwera." 56. Kumeneko ndiko kudzakhala
kusangalala kwawo patsiku lachiweruzo.

57. Ndife amene tidakulengani inu nanga ndi chifukwa
chiyani simukhulupilira? 58. Ndiuzeni za umuna umene
mumatulutsa? 59. Kodi ndinu amene mumaulenga
kapena Ife ndife timaulenga? 60. Ife tidalamulira imfa
kukhala pakati panu ndipo Ife sitingagonjetsedwe ayi
61. Kukusinthani inu ndi kukulengani kukhala china chake
chimene inu simuchidziwa. 62. Ndithudi inu mumadziwa
za chilengedwe choyamba. Nanga ndi chifukwa chiyani
simulabadira? 63. Kodi mudayamba mwaganiza za mbewu
imene mumabzala? 64. Kodi ndinu amene mumaimeretsa

kapena ndife amene timameretsa? 65. Ngati titafuna, Ife
tikadaiphwanya m'timagawomagawo touma ndipo inu
mukadayamba kudandaula. 66. Ndithudi ife tapatsidwa
chingongole cholemera. 67. Iyayi. Koma tamanidwa.
68. Kodi inu mumawaona madzi amene mumamwa?
69. Kodi ndinu amene mumawagwetsa kuchokera ku
mitambo kapena ndife? 70. Chikadakhala chifuniro chathu
tikadawapanga iwo kukhala a mchere. Nanga ndi chifukwa
chiyani simuthokoza? 71. Kodi inu mumaganizira za moto
umene mumasonkha? 72. Kodi ndinu amene mumameretsa
mtengo umene umayaka moto kapena ndife amene
timaumeretsa? 73. Ife taupanga iwo kukhala chikumbutso
ndi chinthu chothandiza anthu amene ali paulendo.
74. Kotero lemekezani dzina la Ambuye wanu Wamkulu.

75. Ndipo ndilumbira pali nyenyezi zimene zili kugwa.
76. Ndithudi ili ndi lonjezo lalikulu inu mukadadziwa.
77. Ndithudi ndi Buku lolemekezeka la Korani. 78. Limene
lili m'Buku lotetezedwa. 79. Palibe amene adzalikhudza
kupatula oyeretsedwa okha. 80. Chivumbulutso chochokera
kwa Ambuye wa zolengedwa zonse. 81. Kodi muli kunyozabe
uthenga uwu? 82. Mmalo mothokoza chifukwa cha zinthu
zimene amakupatsani inu mumamukana Iye.

83. Nanga ndi chifukwa chiyani inu simuthandiza pamene
mzimu wa munthu amene ali kufa ufika pa khosi pake?
84. Pamene panthawiyo, inu mumangoyang'ana. 85. Koma Ife
tili pafupi ndi iye kuposa inu koma inu simutiona. 86. Nanga
ndi chifukwa chiyani simutero ngati inu simudzaweruzidwa
patsogolo pake. 87. Bwezerani mzimuwo ngati ndinu anthu a
choonadi. 88. Ndipo ngati iye ndi mmodzi wa anthu amene
ali kufupi ndi Mulungu, 89. Iye adzapeza mpumulo ndi

chakudya ndi munda wa chisangalalo. 90. Ndipo ngati iye
ndi wam'gulu la anthu akudzanja la manja, 91. Kotero kuli
mtendere kwa iwo a kudzanja lamanja. 92. Ndipo ngati iye
ndi mmodzi wa iwo okana choonadi ndi amene amalakwa.
93. Motero kulandiridwa kwake kudzakhala kwa madzi
otentha kwambiri. 94. Ndi kulowetsedwa ku Gahena.
95. Ndithudi ichi ndi choonadi chosakayikitsa. 96. Motero
lemekezani dzina la Ambuye wanu, Wamkulu.

SURA 57 • AL-HADÎD

# AL HADID

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Chilichonse chimwe chili kumwamba ndi padziko lapansi
chimalemekeza Mulungu. Iye ndiye Mwini mphamvu,
Mwini nzeru. 2. Wake ndi Ufumu wakumwamba ndi dziko
lapansi. Ndiye amene amapereka moyo ndi imfa ndipo
ali ndi mphamvu pa zinthu zonse. 3. Iye ndi woyamba ndi
womaliza, wapamwamba mwamba ndi wapafupi. Ndipo Iye
amadziwa zinthu zonse. 4. Ndiye adalenga kumwamba ndi
dziko lapansi m'masiku asanu ndi limodzi ndipo adabuka
pa mwamba pa mpando wake wa Chifumu. Iye amadziwa
chilichonse chimene chimalowa m'nthaka ndi chilichonse
chimene chimatuluka mu iyo, zonse zimene zimadza
pansi kuchokera kumwamba ndi zonse zimene zimakwera
kumwamba. Ndipo Iye ali nanu kulikonse kumene
mungakhale. Ndipo Mulungu amaona zonse zimene

mumachita. 5. Wake ndi Ufumu wakumwamba ndi dziko
lapansi. Ndipo ndi kwa Iye kumene zonse zimabwerera.
6. Iye amapanga usiku kulumikizana ndi usana ndi kupanga
usana kulumikizana ndi usiku. Iye amadziwa zinsinsi zonse
zili m'mitima.

7. Khulupiririrani mwa Mulungu ndi Mtumwi wake.
Perekani zopereka zaulere kuchokera ku zinthu zimene
Mulungu wakupatsani kuti zikhale zanu. Iwo a inu amene
akhulupilira ndipo apereka chaulere, yawo idzakhala
mphotho yaikulu. 8. Kodi ndi chifukwa chiyani kuti inu
simukhulupirira mwa Mulungu? Pamene Mtumwi ali
kukuitananí kuti mukhulupirire mwa Ambuye wanu ndipo
Iye, ndithudi, walandira lonjezo lanu ngati inu ndinu anthu
okhulupirira. 9. Ndiye amene amatumiza kwa kapolo
wake zizindikiro zooneka kuti akhoza kukutsogolerani
inu kuchoka ku mdima waukulu kupita kowala. Ndipo,
ndithudi, Mulungu, kwa inuyo, ndi wachifundo ndi
wachisoni. 10. Kodi ndi chifukwa chiyani inu simufuna
kupereka m'njira ya Mulungu? Mulungu ndiye Mwini wa
zonse zili kumwamba ndi padziko lapansi. Palibe ofanana,
pakati panu, ndi iwo amene amapereka chaulere ndipo
adamenya nawo nkhondo poyamba kupambana kusanadze.
Amenewa ndi a pamwamba kuposa iwo amene adapereka
chaulere ndi kumenya nkhondo pambuyo pake. Koma kwa
onsewa, Mulungu walonjeza mphotho yokoma. Ndipo
Mulungu amadziwa zonse zimene mumachita.

11. Kodi ndani amene adzakongoza Mulungu ngongole
yabwino kuti Iye aipindulitse ndipo kuti iye adzakhale
ndi mphotho ina yapamwamba? 12. Patsiku limeneli inu
mudzaona amuna okhulupirira ndi akazi okhulupirira,

nyali zawo zili kuyaka patsogolo pawo ndi kudzanja lawo
lamanja, kulonjerana kwawo kudzakhala nkhani yabwino
kwa inu lero lino! Minda imene pansi pake pamayenda
madzi mudzakhala m'menemo mpaka kalekale. Kumeneko
ndiko kupambana kwenikweni. 13. Patsiku limene amuna
a chinyengo ndi akazi a chinyengo adzanena kwa iwo
okhulupirira: "Tidikirireni kuti tikhoza kulandira chilangali
kuchokera ku muuni wanu." Koma kudzanenedwa kuti:
"Bwererani m'mbuyo kuti mukafune muuni wanu. Ndipo
chipupa chidzakhazikitsidwa pakati pawo chokhala
ndi khomo. Mbali ina ya chipupachi kudzakhala
chisomo pamene mbali ina kudzakhala chilango."
14. Iwo adzalira kwa iwo. "Kodi inu sitinali kukhalira
limodzi?" Okhulupilira adzayankha kuti: "Zoonadi koma
inu mudadzisocheretsa nokha. Inu mudanyengedwa,
mudakayikira ndipo zilakolako zanu zidakunyengani
inu mpaka pamene chilango cha Mulungu chinachitika.
Ndipo wonyenga adakunyengani inu pa nkhani zokhudza
Mulungu." 15. Motero lero palibe chiphuphu chimene
chidzalandiridwa kuchokera kwa inu kapena iwo amene
adakana Mulungu. Malo anu okhala ndi kumoto, amenewo
ndiwo malo okhawo amene mudzalandiridwako ndipo ndi
malo oipitsitsa kukhalamo.

16. Kodi nthawi siinakwane yoti okhulupirira
enieni apereke mitima yawo modzichepetsa ndipo
kuti azikumbukira Mulungu ndi choonadi chimene
chavumbulutsidwa kwa iwo ndipo kuti asakhale ngati iwo
amene adapatsidwa Buku nthawi ya kale? Koma patapita
nthawi, mitima yawo idalimba. Ndipo ambiri a iwo ndi
ophwanya malamulo. 17. Dziwani kuti Mulungu amapereka

moyo ku nthaka ikafa. Ndithudi taonetsa chivumbulutso chathu poyera kwa inu kuti mukhoza kuzindikira.

18. Ndithudi iwo amene amapereka chopereka chaulere, amuna kapena akazi, iwo amasunga gawo lawo kwa Mulungu lomwe lidzaonjezeredwa mopitiriza muyeso ndipo adzakhala ndi mphotho yolemekezeka.
19. Ndipo iwo amene amakhulupirira mwa Mulungu ndi mwa Mtumwi wake, iwo ndi olungama ndi okhulupirira pamaso pa Ambuye wawo. Iwo adzalandira mphotho yawo pamodzi ndi muuni. Ndipo iwo amene sakhulupirira ndipo amakana chivumbulutso chathu, amenewa ndiwo a ku moto wa ku Gahena.

20. Dziwani kuti moyo wa padziko lino lapansi ndi masewera ndi wotailako nthawi, chionetsero ndi kunyada ndi mpikisano pakati pa wina ndi mnzake wofuna chuma ndi ana. Fanizo lake lili ngati mvula ndi zomera zimene zimadza chifukwa cha zimene zimabweretsa chisangalalo kwa ozilima. Pasanapite nthawi izo zimafota ndi kuoneka za chikasu. Ndipo zimauma ndi kugwa pansi. Koma m'moyo umene uli kudza, kuli chilango chowawa kwa anthu ogona m'machimo ndi chikhululukiro chochokera kwa Mulungu ndiponso chisangalalo chake kwa iwo amene amadzipereka kwa Mulungu. Kodi moyo wa padziko lino lapansi ndi chiyani kupatula chinyengo chabe?
21. Kotero fulumirani kupeza chikhululukiro cha Mulungu ndi munda wa Paradiso umene kutalika kwake kuli ngati kukula kwa kumwamba ndi dziko lapansi umene udakonzedwera iwo amene amakhulupirira mwa Mulungu ndi Atumwi ake. Chimenechi ndicho chisomo cha Mulungu chimene

amapereka kwa amene Iye wamufuna. Mulungu ndi
Ambuye wa chisomo chosatha.
22. Palibe vuto limene limadza padziko kapena pa inu
limene silinakhazikitsidwe kale Ife tisanalibweretse.
Ndithudi chimenechi ndi chosavuta kwa Mulungu.
23. Kuti inu musakhumudwe chifukwa cha zinthu zabwino
zimene simudazipeze kapena kunyada chifukwa cha
zokoma zimene zaperekedwa kwa inu. Mulungu sakonda
anthu odzikundikira. 24. Ndiponso anthu a umbombo
amauza anzawo kuti nawonso azikhala a umbombo.
Ngati wina abwerera m'mbuyo kuchokera ku njira ya
Mulungu, ndithudi, Mulungu sasowa chilichonse ndipo ndi
wolemekezeka.
25. Ndithudi tidatumiza kale Atumwi athu ndi zizindikiro
zooneka ndipo tidatumiza pamodzi ndi iwo Buku ndi
muyeso kuti anthu akhoza kukhala ndi makhalidwe abwino.
Ndipo Ife tidapanga chitsulo chimene m'kati mwake muli
mphamvu ndi zinthu zambiri zabwino kwa anthu. Kuti
Mulungu akhoza kuyesa iwo amene amamuthandiza Iye
ndi Mtumwi wake mwamseri. Ndithudi Mulungu ndi
wolimba ndi wamphamvu.
26. Ndithudi Ife tidatumiza Nowa ndi Abrahamu ndipo
tidapereka kwa ana awo mphatso ya Utumwi ndi Buku
ndipo ena pakati pawo ndi otsogozedwa bwino koma
ambiri ndi ophwanya malamulo. 27. Ndipo tidawapanga
Atumwi athu kuti atsatire m'mapazi mwawo; Ndipo
tidatumiza Yesu, mwana wa Maria, pambuyo pake ndipo
tidamupatsa Uthenga Wabwino. Ndipo tidaika m'mitima
mwa iwo amene adali kumutsatira iye kukoma mtima ndi
chisoni. Ukakhala unsembe iwo adapeka okha, chifukwa Ife

sitidawalamulire kuti akhazikitse kupatula kuti azifunafuna
chisangalalo cha Mulungu koma iwo sadazilabadire ayi.
Kotero tidawapatsa mphotho iwo amene adakhulupirira
koma ambiri a iwo ndi oswa malamulo.
28. Oh inu anthu okhulupirira! Samalani udindo wanu
kwa Mulungu ndipo mukhulupilire mwa Mtumwi wake.
Iye adzakupatsani magawo awiri a chisomo chake
ndikukonzerani muuni umene muzidzayenda nawo
ndi kukukhululukirani machimo anu. Mulungu ndi
wokhululukira ndi wachisoni chosatha. 29. Kuti anthu a
m'Buku adziwe kuti iwo alibe mphamvu ina iliyonse pa
chisomo cha Mulungu ndipo kuti chisomo chake chili
m'manja mwake mokha ndipo amachipereka kwa aliyense
amene Iye wamufuna. Mulungu ndiye Mwini mphatso
zosatha.

SURA 58 • AL-MUJÂDILAH

# AL MUJADILAH

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ndithudi Mulungu wamva mau a mkazi amene ali
kutsutsana ndi iwe pa nkhani ya mwamuna wake ndipo iye
wapereka madandaulo ake kwa Mulungu. Ndipo Mulungu
wamva kukangana kwanu chifukwa Iye amamva ndiponso
amaona chili chonse.
2. Iwo amene ali pakati panu ndipo amasudzula akazi
awo ponena kuti: "Iwe uli ngati msana wa Amai anga." Iwo

sangakhale Amai awo ai. Palibe amene angakhale amayi
awo, kupatula okhawo amene anawabara. Ndithudi iwo
amalankhula mau oipa ndi bodza. Ndithudi Mulungu
amakhululukira nthawi zonse. 3. Ndipo iwo amene
amasudzula akazi ponena kuti amaoneka ngati kumbuyo
kwa amayi awo kenaka afuna kuti akhululukidwe pa
zomwe adanena ayenera kumasula kapolo asanabwererane.
Limeneli ndi lamulo limene mwalamulidwa kuti
mulimvere ndipo Mulungu amadziwa chilichonse chimene
mumachita. 4. Ndipo ngati wina sangathe kutero, ayenera
kusala chakudya miyezi iwiri mosadukiza asanabwererane.
Koma ngati sangathe kutero, ayenera kudyetsa anthu
osauka makumi asanu ndi limodzi; ndi cholinga chakuti
muonetse chikhulupiriro mwa Mulungu ndi Mtumwi wake.
Amenewa ndiwo malamulo amene adakhazikitsidwa ndi
Mulungu. Ndipo kwa anthu osakhulupilira kuli chilango
chowawa.

5. Ndithudi onse amene amatsutsa Mulungu ndi Mtumwi
wake adzatsitsidwa kwambiri monga momwe adatsitsidwira
iwo amene adalipo kale. Ndipo Ife tatumiza zizindikiro
zooneka. Ndipo anthu onse osakhulupirira adzalandira
chilango chochititsa manyazi. 6. Patsiku limene Mulungu
adzawaukitsa onse kwa akufa ndi kuwauza ntchito zawo
zonse zimene adachita. Mulungu anasunga zimene iwo
adaiwala. Ndipo Mulungu ndi mboni pazinthu zonse.

7. Kodi iwe siudaone kuti Mulungu amadziwa zonse
zimene zili mlengalenga ndi chilichonse chimene chili
padziko lapansi? Palibe nkhani za chinsinsi pakati pa anthu
atatu zimene Iye sakhala wachinayi, kapena pakati pa
anthu asanu pamene Iye sakhala wa chisanu ndi chimodzi,

kapena pakati pa anthu ochepa kapena ochuluka, koma
Iye amakhala pakati pawo. Kulikonse kumene iwo
angakhale pomaliza Iye adzawauza zonse zimene adachita
patsiku lachiweruzo. Ndithudi Mulungu amadziwa
chilichonse. 8. Kodi iwe siudawaone amene adaletsedwa
kuchita misonkhano ya mseri komabe amayambanso
kuchita misonkhano ya chinsinsi imene adaletsedwa kuti
asamachite? Iwo amachita misonkhano pakati pawo ndi
cholinga choukira ndi kusamvera Mtumwi wa Mulungu.
Koma iwo akamadza kwa iwe, iwo amakulonjera iwe
osati monga mmene Mulungu amakulonjerera ayi koma
mwachinyengo. Ndipo iwo amati kwa wina ndi mnzake:
“Kodi bwanji Mulungu satilanga pa zimene timanena?”
Gahena ndi yokwana kwa iwo, ndipo adzapsa m’malawi
ake. Ndipo kumeneko ndi konyansa kwambiri.
9. Oh inu anthu okhulupirira! Pamene inu muchita
misonkhano yanu yamseri musalankhule zinthu zoipa,
zoukira ndi zosamvera Mtumwi koma muzilankhula
zinthu zachilungamo ndi zamvano. Ndipo muopeni
Mulungu chifukwa ndi kumene nonse mudzabwerera.
10. Misonkhano yamseri imachokera kwa Satana amene
amafuna kusokoneza anthu okhulupirira. Koma Iye
sangawalakwitse ayi kupatula ndi chilolezo cha Mulungu
ndipo mwa Mulungu ndi momwe anthu okhulupirira
ayenera kuika chikhulupiriro chawo.
11. Oh inu anthu okhulupirira! Ngati muuzidwa kukonza
malo m’misonkhano yanu, konzani malo okwanira. Ndipo
Mulungu adzakukonzerani inu malo okwanira kwambiri.
Ndipo mukauzidwa kuti mudzuke, dzukani. Mulungu
adzakweza mu maudindo ena a inu amene mukhulupirira

ndi iwo amene apatsidwa nzeru. Ndipo Mulungu amadziwa
ntchito zanu zonse.
12. Oh inu anthu okhulupirira! Ngati mufuna kukumana
ndi Mtumwi mwamseri, perekani chaulere chanu
musanayambe kukambirana naye. Zimenezo zidzakhala
zabwino kwa inu ndiponso dongosolo. Koma ngati inu
mulibe chopereka, Mulungu ndi wokhululukira ndi Mwini
chisoni chosatha. 13. Kodi inu muli kuchita mantha kupereka
chaulere chanu musanakumane naye? Ngati nditero,
musachite mantha chifukwa Mulungu wakukhululukirani.
Motero pitirizani kupemphera nthawi zonse, perekani
msonkho wothandiza osauka, ndipo mverani Mulungu ndi
Mtumwi wake. Ndithudi Mulungu amadziwa ntchito zanu
zonse.
14. Kodi iwe suwaona amene amapalana ubwenzi ndi
anthu amene adalandira mkwiyo wa Mulungu? Iwo si a
m'gulu lako kapena a mgulu lawo, ndipo iwo amalumbira
zabodza pamene ali kudziwa. 15. Mulungu wawakonzera
chilango chowawa. Ndithudi zoipa ndizo anali kuchita.
16. Iwo apanga malonjezo awo kukhala chishango. Kotero
iwo amatchinjiriza anthu ku njira ya Mulungu ndipo iwo
adzalandira chilango chochititsa manyazi.
17. Chuma kapena ana awo sizidzawathandiza ku mkwiyo
wa Mulungu. Iwo adzapita kumoto kumene adzakhaleko
mpaka kalekale. 18. Patsiku limene Mulungu adzawadzutsa
onse, iwo adzalumbira pamaso pake monga momwe
alumbirira kwa inu. Ndipo iwo amaganiza kuti ali ndi
mtsamiro. Ndithudi iwo ndi abodza. 19. Satana ndiye
ali kuwalamulira. Ndipo wawachititsa iwo kuti aiwale
kukumbukira Mulungu. Iwo ali m'gulu la Satana. Ndithudi

gulu la Satana lidzakhala lolephera. 20. Iwo amene amatsutsa
Mulungu ndi Mtumwi wake adzakhala pakati pa anthu
amene adzanyozedwa zedi. 21. Mulungu walamulira kuti:
Ndithudi! Ine pamodzi ndi Atumwi anga tidzapambana.
Ndithudi Mulungu ndi wamphamvu zonse.
22. Iwe sudzapeza anthu amene amakhulupirira mwa
Mulungu ndi tsiku lomaliza ali kuchita chibwenzi ndi iwo
amene amatsutsa Mulungu ndi Mtumwi wake ngakhale
kuti atakhala abambo wawo, kapena ana awo kapena
abale awo kapena anansi awo. Kwa awa, Iye wakhazikitsa
chikhulupiriro m'mitima mwawo, ndipo wawalimbikitsa
ndi ulangizi, wochokera kwa Iye. Ndipo Iye adzawalandira
m'minda ya Paradiso, imene pansi pake pamayenda
mitsinje kuti akhale komweko mpaka kalekale. Mulungu
wasangalala nawo ndipo nawonso asangalala ndi Iye. Iwo
ndi anthu a gulu la Mulungu. Ndithudi ndi anthu a Mulungu
amene adzapambana.

Sura 59 • Al-Hashr

# Al Hashr

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Chilichonse chimene chili kumwamba ndi padziko
lapansi chimalemekeza Mulungu. Ndipo Iye ndiye Mwini
mphamvu zonse ndi wanzeru. 2. Ndiye amene adachotsa
anthu osakhulupirira amene adali pakati pa anthu a m'Buku
kuchokera ku nyumba zawo pamene adakumana poyamba.

Iwe sumaganiza ndi pang'ono pomwe kuti angachoke.
Ndipo iwo anali kuganiza kuti Malinga awo adzawateteza
kwa Mulungu! Koma chilango cha Mulungu chidadza pa
iwo kuchokera kumbali imene iwo sanali kuyembekezera.
Ndipo Iye adaika mantha m'mitima mwawo kotero iwo
adagwetsa nyumba ndi manja awo ndiponso manja a anthu
okhulupirira. Motero chenjerani tsopano inu amene muli
ndi maso.

3. Ngati Mulungu akadapanda kuwalamulira kuti
achotsedwe, ndithudi, Iye akanawalanga m'dziko lomwe
lino ndipo m'moyo umene uli nkudza, ndithudi, iwo
adzalandira chilango cha ku Gahena. 4. Chifukwa iwo
adatsutsa Mulungu ndi Mtumwi mwake. Ndipo ngati wina
atsutsa Mulungu ndi Mtumwi wake, ndithudi, Mulungu
ali ndi chilango choopsa. 5. Chilichonse chimene mudula
cha mitengo ing'ono ing'ono ya tende kapena muisiya
kuti ikhale njo pa mizu yake, mumachita ndi chilolezo
cha Mulungu, ndi cholinga choti achititse manyazi anthu
ochita zoipa.

6. Chimene Mulungu wapereka kwa Mtumwi wake ndipo
walanda kuchokera kwa iwo, si ndinu amene mudapereka
akabvalo kapena ngamira kwa iwo. Koma Mulungu
ndiye amene amapereka mphamvu kwa Mtumwi wake
kupambana aliyense amene iye wafuna ndipo Mulungu
ali ndi mphamvu pa chilichonse. 7. Chilichonse chimene
Mulungu wapereka ngati chuma chopeza pa nkhondo kwa
Mtumwi wake, kuchokera kwa anthu a m'mizinda, mwini
wake ndi Mulungu, Mtumwi wake ndi abale ndi amasiye, ndi
anthu osauka, ndi a paulendo ndi cholinga choti asakhale
katundu wa anthu olemera amene ali pakati panu. Kotero

landirani zimene Mtumwi akupatsani ndipo mulewe
chimene akuletsani. Ndipo opani Mulungu. Ndithudi
Mulungu amalanga molapitsa. 8. Ndi wa amphawi amene
adabwera ndi Mtumwi amene adapilikitsidwa m'nyumba
zawo ndi katundu wawo pofunafuna chisomo chochokera
kwa Mulungu ndi chisangalalo chake. Ndipo amatsatira
Mulungu ndi Mtumwi wake. Amenewa, ndithudi, ndiwo
olungama.
9. Ndipo iwo ndi amene, awa asadadze, adali ndi nyumba
zawo ndipo adalowa Chisilamu, ndipo adaonetsa chikondi
kwa iwo amene amadza kwa iwo, ndipo samachita
kaduka ndi katundu amene aperekedwa kwa iwo koma
amalolera kuti iwo akhale otsiliza polandira ngakhale kuti
nawonso amazifuna. Ndipo aliyense amene amadziteteza
ku zilakolako zake, ndithudi, iye adzakhala opambana.
10. Ndipo iwo amene adadza pambuyo pawo adati: "Ambuye
wathu, tikhululukireni ife pamodzi ndi abale athu amene
adalowa Chisilamu poyambirira, ndipo musasiye m'mitima
mwathu kaduka wowachitira iwo amene adakhulupirira
kale. Ambuye wathu! Ndithudi inu ndinu okoma mtima,
Mwini chifundo."
11. Kodi iwe sudawaone anthu a chinyengo ali kunena
kwa abale awo osakhulupirira amene ali pakati pa anthu
a m'Buku? (Ponena kuti): "Ngati iwo akupirikitsani inu,
nafenso tidzapita nanu, ndipo sitidzamvera wina aliyense
wodana ndi inu. Ngati inu muputidwa, ndithudi, ife
tidzakuthandizani." Koma Mulungu achitira umboni
kuti, ndithudi, iwo ndi abodza. 12. Ndithudi ngati iwo
apirikitsidwa, iwo sadzapita nawo ayi ndipo ngati inu
muputidwa iwo sadzakuthandizani konsekonse. Ndipo

ngati iwo atathandiza, iwo adzangobwerera m'mbuyo
motero iwo sadzapambana ai.
13. Ndithudi inu mumayambitsa mantha m'mitima
mwawo kuposa Mulungu. Ichi ndi chifukwa chakuti iwo ndi
anthu osazindikira. 14. Iwo sadzamenyana nawe ngati gulu
limodzi ayi koma mozemba pogwiritsa ntchito Malinga ya
m'mizinda kapena pobisala kuzipupa. Mtima womenya
nkhondo ulipo pakati pawo moti iwe ukhoza kuganiza
kuti ndi ogwirizana. Koma mitima yawo ndi yogawikana
chifukwa iwo ndi anthu osadziwa chilichonse.
15. Iwo ali ngati amene adadza pambuyo pawo amene
adalandira dipo loipa chifukwa cha ntchito zawo ndipo
iwo adzalandira chilango chowawa kwambiri. 16. Monga
Satana pamene amamuuza munthu kuti: "Usakhulupirire
mwa Mulungu." Ndipo pamene munthu sakhulupirira
mwa Mulungu, Satana amati: "Ndathana nawe tsopano
chifukwa ine ndimaopa Mulungu, Ambuye wazolengedwa
zonse." 17. Motero mapeto awo ndi akuti onsewa adzapsa
ku moto kumene adzakhalako mpaka kalekale. Limenelo
ndilo dipo la anthu ochita zoipa.
18. Oh inu anthu okhulupirira! Opani Mulungu. Ndipo
kwaniritsani udindo wanu kwa Iye. Ndipo ulekeni mzimu
uliwonse uganize zimene udzalandire mawa ndipo opani
Mulungu. Ndithudi Mulungu amadziwa chilichonse
chimene mumachita. 19. Ndipo inu musakhale ngati iwo
amene adaiwala Mulungu ndipo Iye adawachititsa kuti
adziiwale eni ake. Amenewa ndiwo amene amaphwanya
malamulo mopitiriza. 20. Anthu a ku Gahena siofanana
ndi anthu a ku Paradiso. Ndi anthu a ku Paradiso amene
adzakhala opambana.

21. Ife tikadatumiza Buku la Korani ili pa phiri, ndithudi; iwe ukadaona ilo lili kudzichepetsa ndi kung'ambika chifukwa cha mantha ndi Mulungu. Zimenezi ndi zitsanzo zimene timaulula kwa anthu kuti atha kuganiza. 22. Iye
ndiye Mulungu ndipo kupatula Iye kulibe Mulungu wina amene amadziwa zinthu zonse zachinsinsi ndi zolankhula mokweza. Iye ndi Wachifundo, Mwini chisoni chosatha.
23. Iye ndiye Mulungu ndipo kupatula Iye kulibe Mulungu wina. Iye ndi Mwini Ufumu, Woyera, Maziko a mtendere, Mtetezi ndi Mwini ukulu. Ulemerero ukhale kwa Mulungu kuposa zimene amamusinjirira. 24. Iye ndi Mulungu,
Namalenga, Chiyambi ndi Mkonzi. Ake ndi mayina abwino okhaokha. Chilichonse chimene chili kumwamba ndi padziko lapansi chimamulemekeza ndi kumuyamika ndipo Iye ndi Wolemekezeka, Wamphamvu ndi Wanzeru.

Sura 60 • Al Mumtahanah

# Al Mumtahana

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Oh inu anthu amene mwakhulupirira! Musasandutse adani anga ndi adani anu kukhala abwenzi anu powaonetsa chikondi chanu pamene iwo akana choonadi chimene chadza kwa inu ndipo amupirikitsa Mtumwi pamodzi ndi inu nomwe kuchokera ku nyumba zanu, chifukwa chakuti inu mumakhulupirira mwa Mulungu Ambuye wanu. Ngati inu mwadza ndi cholinga chogwira ntchito m'njira

yanga ndi kufunafuna chisangalalo changa(musachite nawo ubwenzi). Ndipo ngati inu mumaonetsa chikondi kwa iwo mwamseri, ndithudi, mukatero mwasochera. Ine ndimadziwa zonse zimene mumachita mseri. 2. Ngati iwo akupambanani, ndithudi, adzakuonetsani kuti ndi adani anu ndipo adzagwiritsa ntchito manja awo ndi malirime awo pa inu pokuchitirani zoipa. Iwo afunitsitsa kuti nanu mukhale anthu osakhulupirira. 3. Abale anu kapena ana anu sadzakhala a phindu kwa inu patsiku la chiweruzo. Iye adzaweruza pakati panu chifukwa Mulungu amaona zonse zimene mumachita.

4. Muli chitsanzo chabwino kwa inu mwa Abrahamu ndi mwa iwo amene adali naye pamene iwo ananena kwa anthu awo kuti: "Ife sitili m'gulu lanu ndipo sitipembedza zimene inu mumapembedza pozifanizira ndi Mulungu. Ife takukanani ndipo pabuka pakati pa ife ndi inu udani ndi chidani chosatha kupatula ngati inu mukhulupirira mwa Mulungu ndi mwa Iye yekha." Kupatula zonena za Abrahamu kwa Abambo ake kuti: "Ine ndidzapempha chikhululukiro chanu chifukwa ine ndilibe mphamvu pa chilichonse cha inu kuchokera kwa Mulungu. Ambuye wathu, mwa Inu ife takhulupirira ndi kwa Inu ndiko timapempha chikhululukiro, ndipo kwa Inu ndiko kumene tonse tidzabwerera pomaliza." 5. "Ambuye wathu, musatisandutse ife kukhala mayesero a anthu osakhulupirira koma tikhululukireni Ambuye wathu. Ndithudi Inu ndinu Mwini mphamvu zonse ndi Mwini nzeru zonse." 6. Ndithudi, mwa iwo mudali chitsanzo chabwino kwa inu kuti mutsatire, makamaka iwo amene amaika chikhulupiriro chawo mwa Mulungu ndi m'tsiku la

chiweruzo. Ndithudi Mulungu ndi wolemera ndipo ndiye
yekha amene ayenera kulemekezedwa. 7. Mwina Mulungu
angakhazikitse chikondi pakati pa inu ndi iwo amene inu
mumawaganizira kuti ndi adani anu. Ndithudi Mulungu
ali ndi mphamvu pa china chilichonse ndipo Mulungu ndi
wokhululukira ndi Mwini chisoni chosatha.
8. Mulungu sali kukuletsani kuti muonetse chilungamo
ndi chisoni kwa iwo amene sadamenyane nanu chifukwa
cha chikhulupiliro chanu ndipo sanakuthamangitseni mu
nyumba zanu. Ndithudi, Mulungu amakonda iwo amene
amachita zolungama. 9. Mulungu wakuletsani kuchita
ubwenzi ndi anthu amene munamenyana nawo chifukwa
cha chikhulupiriro ndipo anakuthamangitsani ku nyumba
zanu kapena adathandiza anthu ena kuti amenyane ndi
kukupirikitsani inu. Ndipo aliyense amene achita ubwenzi
ndi anthu otere ndi ochimwa.
10. Oh inu anthu okhulupirira! Pamene akazi okhulupirira
adza kwa inu ngati othawa mavuto, afufuzeni bwinobwino.
Mulungu yekha ndiye amene adziwa bwino bwino
chikhulupiriro chawo. Ngati inu mukhutitsidwa kuti ndi
okhulupirira m'choonadi, musawabwezere kwa anthu
osakhulupirira chifukwa iwo saloledwa kukwatiwa ndi
anthu osakhulupirira monga momwe amuna osakhulupirira
saloledwa kukwatira akazi okhulupirira. Koma abwezereni
anthu osakhulupirira ziwongo zimene apereka. Ndipo
sikulakwa ngati inu muwakwatira akazi okhulupirirawa
ngati mwapereka chiwongo. Musapitilize ukwati wanu ndi
akazi wosakhulupirira. Itanitsani zimene mwaononga ngati
chiwongo cha ukwati ndipo aloleni osakhulupirira kuti
nawonso aitanitse zimene aononga pa akazi okhulupirira

amene adza kwa inu. Ili ndi lamulo la Mulungu. Iye amaweruza mwachilungamo pakati panu. Mulungu ndi wa nzeru ndi luntha. 11. Ndipo ngati ena, mwa akazi anu, athawa ndi kukakwatiwa ndi osakhulupirira, ndipo inu mupeza mwayi wolandira akazi wochokera kwa anthu osakhulupirira abwezereni chiwongo ndi china chilichonse chimene iwo adapereka anthu amene akazi awo awathawa. Ndipo opani Mulungu amene inu mumamukhulupirira.

12. Oh iwe Mtumwi! Ngati akazi okhulupirira adza kwa iwe kudzalumbira lonjezo lakuti sadzamufanizira Mulungu ndi wina wake akamapembedza, kuti sadzaba, sadzachita chigololo, sadzapha ana awo, sadzalankhula mawu ojeda, sadzapeka nkhani zabodza ndipo kuti adzakumvera iwe pa nkhani ina iliyonse, iwe uyenera kulandira lonjezo lawo ndipo pempha kwa Mulungu kuti awakhululukire machimo awo chifukwa Mulungu ndi wokhululukira ndi Mwini chisoni chosatha.

13. Oh inu okhulupirira! Musapalane ubwenzi ndi anthu amene adalandira mkwiyo wa Mulungu. Ndithudi iwo ali ndi mantha ndi zimene zidzawachitikira m'moyo umene uli nkudza monga momwe anthu osakhulupirira amachitira mantha ndi iwo amene adaikidwa m'manda.

# As-Saff

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Chilichonse chimene chili mlengalenga ndi padziko
lapansi, chimalemekeza Mulungu. Ndipo Iye ndiye Mwini
mphamvu zonse ndi Mwini nzeru. 2. Oh inu okhulupirira!
Kodi bwanji mumanena zinthu zimene simuchita?
3. Ndithudi ndi chinthu chonyansa kwambiri pamaso pa
Mulungu kuti muzinena chinthu chimene simuchita.
4. Ndithudi Mulungu amakonda iwo amene amamenya
nkhondo ndi cholinga chokhazikitsa ulamuliro wake
molimba, m'magulu, ngati chipupa cha miyala.
5. Ndi pamene Mose adanena ndi anthu ake: "Oh inu
anthu anga! Kodi bwanji mukundikwiyitsa pamene muli
kudziwa kuti ine ndine Mtumwi wa Mulungu kwa inuyo?"
Ndipo pamene iwo adalakwa, Mulungu adalola kuti mitima
yawo ilakwe. Ndipo Mulungu satsogolera anthu ophwanya
malamulo.
6. Ndi pamene Yesu, mwana wa mwamuna wa Maria,
adati: "Oh inu ana a Israyeli! Ine ndine Mtumwi wa
Mulungu amene ndatumidwa kwa inu, kutsimikizira za
Buku la Chipangano chakale limene lidadza ine ndisanadze,
ndi kuulula nkhani yabwino ya Mtumwi Ahmad amene
adzabwera ine nditachoka." Koma pamene iye adadza
kwa iwo ndi zizindikiro zooneka, iwo adati: "Awa ndiwo
matsenga enieni." 7. Kodi amalakwa kwambiri ndani kuposa

iye amene amapeka bodza lokhudza Mulungu ngakhale
pamene ali kuitanidwa kuti alowe Chisilamu? Ndipo
Mulungu satsogolera iwo amene amachita zoipa. 8. Cholinga
chawo ndikufuna kuzimitsa nyali ya Mulungu ndi milomo
yawo. Koma Mulungu adzateteza nyali yake ngakhale
kuti anthu osakhulupirira sakondwera nazo. 9. Ndiye
amene watumiza Mtumwi wake ndi ulangizi ndiponso
chipembedzo choonadi kuti chikhale chapamwamba pa
zipembedzo zina zonse ngakhale kuti anthu osakhulupirira
sakondwera nazo.
10. Oh inu anthu okhulupirira! Kodi ndikulangizeni
malonda apafupi amene angakuomboleni ku chilango
choopsa? 11. Kuti mukhulupirire mwa Mulungu ndi mwa
Mtumwi wake, kuti mudzipereke kwathunthu mu njira ya
Mulungu pogwiritsa ntchito chuma chanu ndi inu eni ake.
Chimenechi ndicho chinthu chabwino kwa inu ngati inu
mukadadziwa. 12. Iye adzakukhululukirani inu machimo anu
ndi kukulandirani m'minda imene pansi pake pamayenda
mitsinje, ndipo adzakulowetsani m'nyumba zokongola
ndi zaulemu za m'Paradiso. Kumeneko, ndithudi, ndiko
kupambana kwenikweni. 13. Ndipo Iye adzakupatsani
madalitso ena amene mumakonda. Chithandizo
chochokera kwa Mulungu ndi kupambana mwamsanga.
Kotero auze nkhani yabwino anthu okhulupirira.
14. Oh inu okhulupirira! Khalani otumikira Mulungu
monga momwe ananenera Yesu, mwana wa mwamuna wa
Maria, kwa ophunzira ake: "Kodi ndani andithandiza ine
potumikira Mulungu?" Iwo adayankha: "Ife ndife othandiza
Mulungu." Kotero ena mwa ana a Israyeli adakhulupirira
pamene ena sadakhulupirire. Motero Ife tidawapatsa

mphamvu iwo amene adakhulupirira zopambana adani awo ndipo iwo adapambanadi.

Sura 62 • Al-Jumu’ah

# Al Jumua

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Chilichonse chimene chili mlengalenga ndi padziko
lapansi chimatamanda ndi kulemekeza Mulungu,
Mfumu ya Mafumu, Woyera, Mwini mphamvu zonse ndi
Mwini nzeru. 2. Ndiye amene adatumiza kugulu la anthu
osaphunzira Mtumwi, wochokera m’gulu lawo, kuwauza
iwo zizindikiro zake, kuwayeretsa ndi kuwaphunzitsa
Buku. Ndithudi iwo anali kuchita zoipa kuyambira kale.
3. Ndipo Iye wamutumiza iye pamodzi ndi ena amene anali
pakati pawo amene sadalowe m’gulu lawo. Ndipo Iye ndi
Wamphamvu ndi Wanzeru. 4. Chimenchi ndicho chisomo
cha Mulungu chimene amachipereka kwa aliyense amene
Iye wamufuna. Ndipo Mulungu ndiye Ambuye wachisomo
chapamwamba chosatha.
5. Fanizo la iwo amene adapatsidwa Buku la Chipangano
Chakale ndipo adalephera kukwaniritsa malamulo ake, lili
ngati Bulu amene amasenza katundu wambiri wolemera
wa mabuku. Loipa ndi fanizo la anthu amene amakana
zizindikiro za Mulungu. Ndipo Mulungu satsogolera
anthu ochita zoipa. 6. Nena: “Oh inu Ayuda! Ngati inu
mumaganiza kuti inu nokha ndinu abwenzi a Mulungu

kusiyana ndi anthu ena, pemphani imfa kuti idze pa inu
ngati ndinu a chilungamo. 7. Koma iwo sadzaipempha iyo
chifukwa cha ntchito zimene manja awo adachita. Ndipo
Mulungu amadziwa onse amene amachita zoipa. 8. Nena:
“Ndithudi imfa imene muli kuopa, ndithudi, idzadza pa
inu ndipo inu mudzabwerera kwa Iye amene amadziwa
zinthu zonse zobisika ndi zooneka ndipo Iye adzakuuzani
zonse zimene munali kuchita.
9. Oh inu anthu okhulupirira! Ngati mumva kuitana
kwa mapemphero a masana a tsiku lachisanu, fulumirani
kukakumbukira Mulungu ndipo siyani ntchito zanu.
Chimenecho ndicho chabwino kwa inu ngati mukadadziwa.
10. Ndipo ngati mapemphero akutha, mukhoza
kumwazikana, padziko kukafunafuna zokoma za Mulungu
ndipo muzikumbukira Mulungu kwambiri kuti mukhale
opambana. 11. Ndipo iwo akaona katundu wa malonda
kapena zinthu zina zosangalatsa, iwo amazithamangira izo
ndi kukusiya wekha uli chiimire pa mapamphero. Nena:
“Zimene Mulungu ali nazo ndi zabwino kwambiri kuposa
katundu wina aliyense wamalonda kapena chisangalalo.”
Mulungu ndiye amene amapereka moolowa manja.

# Al Munafiqun

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pamene anthu a chinyengo amadza kwa iwe amati: "Ife
tichitira umboni kuti iwe, ndithudi, ndiwe Mtumwi wa
Mulungu. Inde Mulungu amadziwa kuti iwe, ndithudi,
ndiwe Mtumwi wake ndipo Mulungu achitira umboni kuti
anthu achinyengo, ndithudi, ndi abodza. 2. Iwo asandutsa
malonjezo awo ngati tchingo. Motero iwo amaletsa anthu
ena kuti atsatire njira ya Mulungu. Ndithudi zimene
iwo amachita ndi zoipa. 3. Ichi ndi chifukwa chakuti iwo
adakhulupirira poyamba ndipo pambuyo pake adayambanso
kusakhulupirira. Motero mitima yawo idatsekedwa ndipo
sazindikira china chilichonse. 4. Ndipo pamene iwe uwaona,
matupi awo amakusangalatsa ndipo pamene iwo alankhula,
iwe umamvera zonena zawo. Iwo ali ngati matabwa amene
aimikidwa pa chipupa. Iwo amaganiza kuti mawu onse
amene amveka amanena za iwo. Iwo ndi adani kotero
chenjera nawo. Matemberero a Mulungu akhale pa iwo!
Kodi iwo asocheretsedwa bwanji kunjira yoyenera? 5. Ndipo
zikanenedwa kwa iwo kuti: "Bwerani kuti mwina Mtumwi
wa Mulungu akupempherereni chikhululukiro kuchokera
kwa Mulungu, " iwo amabwerera m'mbuyo ndipo iwe
umawaona ali kutembenuza nkhope zawo mwachipongwe.
6. Ndi chimodzimodzi kwa iwo kaya iwe uwapemphera
chikhululukiro kapena ayi Mulungu sadzawakhululukira

iwo. Ndithudi Mulungu satsogolera anthu ophwanya
malamulo. 7. Iwo ndiwo amene amati: “Musawapatse china
chilichonse anthu amene ali ndi Mtumwi wa Mulungu kuti
amuthawe.” Koma Mulungu ndiye Mwini wa chuma cha
mlengalenga ndi padziko lapansi koma anthu achinyengo
sadziwa zimenezi. 8. Iwo amati: “Ngati tibwerera ku
Medina, ndithudi, anthu a mphamvu, adzathamangitsa
anthu kuchoka ku Mzindawo.” Koma ulemu, mphamvu ndi
ulemerero ndi wa Mulungu, Mtumwi wake ndi okhulupilira
koma anthu a chinyengo sadziwa chimenechi. 9. Oh
inu okhulupirira! Musalole chuma kapena ana anu kuti
akusokonezeni pokukumbukira Mulungu. Ndipo aliyense
amene achita motero, ndithudi, ndi wotayika. 10. Ndipo
perekani kuchokera ku katundu amene takupatsani imfa
isanadze pa wina wa inu kuti iye asanene kuti: “Oh Ambuye
wanga! Inu mukadandibweza mwa kanthawi kochepa, ine
ndikadapereka chaulere chochuluka kuchokera ku chuma
changa ndikukhala mmodzi wa anthu ochita zabwino.”
11. Ndipo Mulungu sapereka nthawi kwa wina pamene
nthawi yake itakwana. Ndipo Mulungu amadziwa
chilichonse chimene mumachita.

# AL TAGHABUN

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Chilichonse chili mlengalenga ndi padziko lapansi
chimatamanda ndi kulemekeza Mulungu. Iye ndiye Mwini
ufumu ndipo kwake ndi kuyamikidwa ndipo Iye ali ndi
mphamvu pa chilichonse. 2. Ndiye amene adakulengani
inu ndipo ena a inu ndi osakhulupirira pamene ena ndi
okhulupirira. Mulungu amaona zonse zimene mumachita.
3. Iye adalenga kumwamba ndi dziko lapansi mwa
chilungamo ndipo Iye adakulengani ndi kukupatsani
maonekedwe abwino ndipo kwa Iye ndi kumene
mudzabwerera. 4. Iye amadziwa chilichonse chimene chili
kumwamba ndi padziko lapansi ndipo amadziwa zonse
zimene mumabisa ndi zimene mumaulula. Ndithudi
Mulungu amadziwa bwino lomwe zinsinsi za m'mitima
mwanu.

5. Kodi inu simudamve za iwo amene sadakhulupirire kale?
Ndipo iwo adalawa chilango chifukwa chosakhulupilira,
ndipo chawo chidzakhala chilango chowawa kwambiri.
6. Ichi ndi chifukwa chakuti kunadza kwa iwo Atumwi
amene adali ndi zizindikiro zooneka koma iwo adati:
"Kodi ife tizitsogozedwa ndi anthu anzathu?" Kotero
iwo sanakhulupilire ndipo anabwerera m'mbuyo. Koma
Mulungu sasowa kanthu. Ndithudi Mulungu ndi Mwini wa
chilichonse ndi Mwini ulemerero wonse.

7. Anthu osakhulupirira amaganiza kuti sadzaukitsidwa
kwa akufa. Nena: “Inde! Pali Ambuye wanga! Inu, ndithudi,
mudzaukitsidwa kwa akufa ndipo mudzauzidwa zimene
mudachita. Zimenezo ndi za pafupi ndi Mulungu.”
8. Motero khulupirirani mwa Mulungu ndi mwa Mtumwi
wake ndi mu Muuni umene Ife tatumiza. Ndithudi
Mulungu amadziwa chilichonse chimene mumachita.
9. Patsiku limene Iye adzakusonkhanitsani inu nonse, tsiku
losonkhana, tsiku limeneli lidzakhala tsiku la mavuto ndi la
mtendere kwa ena a inu. Ndipo iwo amene amakhulupirira
mwa Mulungu ndipo amachita ntchito zabwino, Iye
adzawakhululukira machimo awo ndipo adzawaika
m’minda imene imathiriridwa ndi mitsinje yoyenda
madzi pansi pake kuti akhale m’menemo mpaka kalekale.
Kumeneko ndiko kupambana kwenikweni. 10. Koma iwo
amene sakhulupirira ndipo amakana ulangizi wathu, iwo
adzakhala ku moto nthawi zonse omwe ndi malo oipitsitsa
kukhalako.

11. Palibe vuto limene limadza popanda chilolezo cha
Mulungu ndipo aliyense amene amakhulupirira mwa
Mulungu, Iye amatsogolera mtima wake ndipo Mulungu
amadziwa chilichonse. 12. Mverani Mulungu ndipo mverani
Mtumwi wake. Koma ngati inu mukana, udindo wa
Mtumwi wathu ndi kukuuzani uthenga wathu momveka
ndi poyera. 13. Mulungu! Kulibe Mulungu wina koma
Iye yekha ndipo mwa Mulungu onse okhulupirira aike
chikhulupiriro chawo.

14. Oh inu okhulupirira! Ndithudi pakati pa akazi ndi
ana anu alipo ena amene ndi adani anu, motero chenjerani!
Koma ngati inu muwakhululukira ndipo simulabadira

zoipa zawo, ndithudi, Mulungu ndi wokhulukulukira nthawi
zonse ndi Mwini chisoni chosatha. 15. Chuma chanu
ndipo ana anu ndi mayesero pamene Mulungu ndiye
amene ali ndi mphotho yaikulu. 16. Kotero kwaniritsani
udindo wanu kwa Mulungu ndipo muopeni Iye kwambiri.
Mverani ndipo mumvere. Ndipo perekani chopereka
chaulere. Chimenecho ndi chabwino kwa inu. Ndipo
aliyense amene asiya umbombo adzakhala wopambana.
17. Ngati mukongoza Mulungu ngongole yabwino, Iye
adzaichulukitsa ndipo adzakukhululukirani machimo anu.
Ndipo Mulungu ndi wokonzeka kuyamika ndi kulipira
ndipo ndi wopilira kwambiri. 18. Wodziwa zonse zobisika
ndi zooneka ndipo ndiye Mwini mphamvu zonse ndi
Mwini nzeru zonse.

Sura 65 • At-Talâ’k

# Al Talaq

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Oh iwe Mtumwi! Ngati usudzula akazi ako, asudzule
potsatira nthawi zawo. Ndipo werenga bwino bwino
masiku awo. Ndipo opani Mulungu Ambuye wanu ndipo
musawapirikitse m’nyumba zawo ndipo iwo asachoke
pokhapokha ngati iwo apalamula mlandu wachigololo.
Amenewa ndiwo malamulo amene akhazikitsidwa ndi
Mulungu. Ndipo aliyense amene aphwanya malamulo
a Mulungu, ndithudi, amapondereza mzimu wake. Inu

simudziwa kuti, mwina, Mulungu adzakukumanizaninso.
2. Ndipo ngati iwo ali pafupi kukwaniritsa nthawi yawo,
mukhoza kuwasunga mwaubwino kapena kuwasiya
mwaulemu. Ndipo itanani mboni ziwiri za chilungamo
kuchokera pakati panu. Ndipo perekani umboni wanu
chifukwa cha Mulungu. Limeneli ndi langizo limene
laperekedwa kwa iye amene amakhulupirira mwa Mulungu
ndi tsiku lomaliza. Ndipo aliyense amene aopa Mulungu,
Iye adzamupulumutsa. 3. Ndipo Iye adzamupatsa
zinthu kuchokera ku mbali imene sanali kuyembekeza.
Ndipo aliyense amene amakhulupirira mwa Mulungu,
Iye adzamupatsa chili chonse. Mulungu, ndithudi,
adzamupatsa iye zofuna zake zonse. Ndithudi Mulungu
adakhazikitsa muyeso wa chilichonse.
4. Ndipo ena akazi anu amene adasiya kupita kumwezi,
kwa iwo nthawi yawo yodikira, ngati inu mukaika, ndi
miyezi itatu ndipo iwo amene anasiyiratu, nthawi yawo
idzakhala chimodzimodzi. Ndipo iwo amene ali ndi akazi
odwala pakati, nthawi yawo idzakhala mpaka pamene
abereka. Ndipo aliyense amene amaopa Mulungu, Iye
adzamuchepetsera mavuto ake. 5. Uwu ndi ulamuliro wa
Mulungu umene wakutumizirani inu. Ndipo aliyense
amene aopa Mulungu, Iye adzamuchotsera zoipa zake.
Ndipo Iye adzamuchulukitsira mphotho yake.
6. Khalani nawo monga momwe inu muli kukhalira,
molingana ndi kupeza kwanu. Musawazunze ndi cholinga
chowasowetsa mtendere. Ngati iwo ali ndi pakati,
asamalireni mpaka pamene iwo abereka. Ndipo ngati iwo
ali kuyamwitsa, apatseni malipiro awo ndipo lemekezanani.
Ndipo ngati pali mavuto oti simuli kugwirizana m'banja,

pezani Mayi wina kuti ayamwitse mwana m'malo mwake.
7. Mulekeni munthu wolemera kuti apereke molingana
ndi chuma chake ndipo munthu wosauka molingana ndi
mmene Mulungu adamupatsira iye. Mulungu sakhazika
mtulo wolemera pa munthu umene sangathe kuunyamula.
Mulungu adzapereka mtendere mavuto akatha.
8. Ndipo ndi mizinda yambiri imene idaukira malamulo
a Mulungu ndi Atumwi ndipo Ife tidayilanga iyo ndipo
tidzailanga ndi chilango choopsa zedi. 9. Motero iyo
idalawa mphotho ya kusakhulupilira kwake ndipo
mapeto a kusakhulupilira adali chionongeko. 10. Mulungu
wawakonzera iwo chilango choopsa. Motero opani Mulungu
oh inu anthu ozindikira! Inu amene mwakhulupirira,
ndithudi, Mulungu watumiza chikumbutso kwa inu.
11. Mtumwi amene ali kukuuzani zizindikiro zooneka
za Mulungu ndi cholinga choti atsogolere onse amene
akhulupirira ndipo amachita ntchito zabwino kuchokera
ku mdima kupita kowala. Ndipo aliyense amene
amakhulupirira mwa Mulungu ndipo amachita ntchito
zabwino, Iye adzamulowetsa m'minda imene pansi pake
pamayenda mitsinje kuti adzakhaleko mpaka kalekale.
Ndithudi Mulungu wawapatsa iwo mphotho yabwino
kwambiri.
12. Ndi Mulungu amene adalenga miyamba isanu ndi
iwiri ndi dziko lapansi lolingana nayo. Malamulo ake
amatsatiridwa ndi izo kuti inu mukhoza kudziwa kuti
Mulungu ali ndi mphamvu pa zinthu zonse ndipo kuti
Mulungu amadziwa chilichonse.

# AL TAHRIM

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Oh iwe Mtumwi! Bwanji ukudziletsa zinthu zimene
Mulungu adakuloleza kuti uchite ndipo iwe ufuna
kukondweretsa akazi ako? Ndipo Mulungu ndi
wokhululukira nthawi zonse, Mwini chisoni chosatha.
2. Mulungu wakulolezani kuti mukhoza kumasula
malonjezo anu. Ndipo Mulungu ndiye Mtetezi wanu,
ndipo ndi wodziwa ndi Mwini nzeru zonse.
3. Ndi pamene Mtumwi anamuuza nkhani ya chinsinsi
wina wa akazi ake ndipo iye adaulula kwa mnzake wina
ndipo Mulungu adamuuza iye za izo, Iye anamuuza gawo
la nkhani ndipo anasiya gawo lina. Ndipo pamene iye
adamuuza mkaziyo za izo, iye adati: "Ndani wakuuzani
izi?" Iye adati: "Wandiuza ndi amene amadziwa
chilichonse ndi Mwini kuzindikira." 4. Ngati inu awiri
mulapa machimo anu kwa Mulungu ndipo mitima yanu
itsimikiza kutero, koma ngati inu mugwirizana kulimbana
naye, ndithudi, Mulungu ndiye Mtetezi wake, ndi Gabriele
ndipo aliyense wolungama amene ali pakati pa anthu
amene akhulupirira ndi angelo. Onse ndi omuthandiza
iye. 5. Zingatheke kuti pamene iye akusudzulani inu,
Mulungu adzamupatsa m'malo mwanu, akazi ena abwino
oposa inu amene amadzipereka kwa Mulungu, amene ali
okhulupirira, opirira, olapa kwa Mulungu, opembedza

modzichepetsa, osala zifuniro zawo, kapena obwera amene anakwatiwapo kale kapena a namwali. 6. Oh inu okhulupirira! Dzitetezeni nokha ndi mabanja anu ku moto umene nkhuni zake ndi anthu ndi miyala ndipo oyang'anira ake ndi angelo a mphamvu a maonekedwe oopsa amene sakana kumvera malamulo amene amalandira kuchokera kwa Mulungu ndipo amachita, mwamsanga, chilichonse chimene Mulungu wawalamula. 7. Oh inu osakhulupirira! Musawiringule lero! Inu muli kulandira mphotho yolingana ndi zimene mudachita! 8. Oh inu anthu okhulupirira! Lapani kwa Mulungu mwachoonadi! Mwina Ambuye wanu angakuchotserani machimo anu ndi kukulowetsani inu m'minda imene pansi pake pamayenda mitsinje. Tsiku limene Mulungu sadzalola kuti Mtumwi ndi iwo amene amamutsatira kuti azunzidwe, nyali yawo idzayaka patsogolo pawo ndi Buku ku dzanja lamanja lawo. Iwo adzati: "Ambuye wathu walitsani nyali yathu ndipo tikhululukireni. Ndithudi inu muli ndi mphamvu pa zinthu zonse."

9. Oh iwe Mtumwi! Limbika kwambiri pogonjetsa anthu osakhulupirira ndi anthu a chinyengo ndipo chita nawo mwankhanza, malo awo ndi kumoto, omwe ndi malo oipa kwambiri kukhalako. 10. Mulungu ali kupereka chitsanzo kwa anthu osakhulupirira cha nkhani ya mkazi wa Nowa ndi mkazi wa Loti. Iwo adali akazi a Atumiki athu awiri a ngwiro, koma onse adanyenga amuna awo. Iwo sadalandire kuchokera kwa Mulungu chabwino china chilichonse chifukwa chamakhalidwe awo. Koma iwo adauzidwa kuti: "Lowani inu kumoto pamodzi ndi ena amene ali kulowako."

11. Ndipo Mulungu wapereka chitsanzo kwa anthu

okhulupirira, nkhani ya mkazi wa Farao. Pamene iye adati: “Oh Ambuye wanga! Ndimangireni pafupi ndi Inu, nyumba ya ulemu ku Paradiso, ndipo ndipulumutseni kwa Farao ndi ntchito zake ndipo ndipulumutseni ine kwa athu amene amachita zoipa.”

12. Ndi Maria mwana wa Imran, amene adadzisunga wosadula unamwali wake ndipo Ife tidauzira m’thupi mwake mzimu wathu ndipo Iye adachitira umboni wachilungamo cha Ambuye wake ndi chivumbulutso chake. Ndipo iye adali mmodzi wa odzipereka kwa Mulungu.

Sura 67 • Al-Mulk

# Al Mulk

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Wodalitsika ndiye amene mmanja mwake muli Ufumu
ndipo ali ndi mphamvu pa zinthu zonse. 2. Iye amene
adalenga imfa ndi moyo kuti akhoza kukuyesani inu kuti ndani wa inu amene wasunga malamulo onse mwaubwino.
Ndipo Iye ndi Wamphamvu ndi Wokhululukira. 3. Iye
ndi amene adalenga miyamba isanu ndi iwiri, wina pamwamba pa unzake. Inu simungaone cholakwa china chilichonse mu chilengedwe cha Mwini chisoni chosatha. Tapenyetsetsani! Kodi inu mungaone cholakwika china
chilichonse? 4. Tapenyetsetsaninso! Ndipo mawonekedwe anu adzakubwererani pamene ali osokonezeka ndi otopa.
5. Ndithudi Ife takongoletsa thambo loyamba ndi nyali

ndipo tazipanga nyalizo ngati mipaliro yothamangitsira Satana ndipo tawakonzera iwo chilango chamoto woyaka. 6. Ndipo iwo amene sakhulupirira mwa Ambuye wawo, kuli chilango cha kumoto ndipo chimaliziro chawo chidzakhala choipa. 7. Ndipo pamene iwo adzaponyedwa m'moto, iwo adzaumva uli kuyaka ndi kubwata. 8. Pafupifupi kuphulika chifukwa cha kukwiya. Ndipo nthawi zonse pamene gulu liponyedwamo, amene amayang'anira moto adzafunsa kuti: "Kodi panalibe wina aliyense amene adadza kwa inu kudzakuchenjezani?" 9. Ndipo iwo adzati: "Inde. Ndithudi Mchenjezi adadza kwa ife koma tidamukana ndipo tinkati: Mulungu sadavumbulutse china chilichonse ndipo iwe ndiwe wosokoneza kwambiri." 10. Ndipo iwo adzati: "Tikadakhala kuti tidamvera kapena kuganiza bwino, ife sitikadakhala m'gulu la anthu opita ku moto." 11. Motero iwo adzabvomera machimo awo. Motero apite kutali anthu a ku moto!.

12. Ndithudi! Iwo amene amaopa Ambuye wawo ngakhale samuona, ndithudi, iwo adzawakhululukira machimo awo ndipo adzalandira mphotho ya mtengo wapatali. 13. Ndipo kaya mubisa mawu anu kapena muulula, Iye amadziwa zonse zimene zili m'mitima mwanu. 14. Kodi Iye amene adalenga zinthu zonse asadziwe? Ndithudi Iye ndi wa Chisoni chosatha ndi Mwini kudziwa chili chonse.

15. Iye ndiye amene anakukonzerani dziko, motero pitani paliponse mu ilo, ndipo idyani zokoma zake zimene wakupatsani ndipo ndi kwa Iye kumene zonse zidzabwerera. 16. Kodi inu mumaganiza kuti ndinu wokhazikika moti Iye amene ali pamwamba pa kumwamba sangathe kung'amba nthaka imene ili pansi panu kuti ikumezeni? Taonani! Ili

kugwedezeka. 17. Kapena mumaganiza kuti inu ndinu
okhazikika kuposa zimene zili kumwamba kuti Iye
sangathe kukutumizirani mphepo ya mkuntho? Kotero inu
mudzadziwa kuopsa kwa chenjezo langa. 18. Ndithudi iwo
amene adalipo kale anakana. Kodi chilango changa chinali
bwanji?

19. Kodi iwo saona mbalame zimene zimauluka pamwamba
pawo, zikutambasula ndi kutseka mapiko awo? Palibe
chimene chimazigwira kupatula Mwini chisoni chosatha.
Ndithudi Iye amaona chilichonse. 20. Kodi ndani amene
angakuthandizeni inu kupatula Mwini chisoni chosatha?
Anthu onse osakhulupirira ndi olakwa. 21. Kodi ndani
amene angakupatseni chisamaliro ngati Iye atakaniza
chisamaliro chake? Koma iwo amapitiriza kuchita mtudzu
ndi kugalukira.

22. Kodi iye amene amayenda osaona ndi ofanana
ndi amene walangizidwa kapena amene amayenda mu
njira yoyenera? 23. Nena: "Ndiye amene adakulengani
inu ndipo adakupatsani makutu, maso ndi mitima. Inu
simuthokoza kawirikawiri." 24. Nena: "Ndiye amene
anakulengani inu kuchokera ku doti ndipo kwa Iye nonse
mudzasonkhanitsidwa."

25. Iwo amati: "Kodi lonjezo limeneli lidzakwaniritsidwa
liti ngati zimene ulikunena ndi zoona?" 26. Nena: "Mulungu
yekha ndiye amene adziwa nthawi yake. Ntchito
yanga ndikungokuchenjezani basi." 27. Koma pamene
iwo adzachiona chili nkudza pafupi, nkhope za anthu
osakhulupirira zidzakhala za chisoni ndipo kudzanenedwa
kuti: "Ichi ndi chimaliziro chimene munkafunsa kuti
chidzafika liti?" 28. Nena: "Ndiuzeni! Kodi ngati Mulungu

atandiononga ine pamodzi ndi iwo amene ali nane,
ngakhale kuti Iye adzaonetsa chifundo pa ife, ndani amene
angateteze anthu osakhulupirira ku chilango chowawa?”
29. Nena: “Iye ndi Mwini chifundo chosatha, mwa Iye ife
timakhulupirira ndipo mwa Iye ife timaika chikhulupiriro
chathu. Kotero inu mudzadziwa posachedwapa kuti ndani
amene ali wochimwa.” 30. Nena: “Ndiuzeni! Kodi ngati
madzi anu ataphwa, ndani amene angakupatseni inu madzi
oyenda?”

Sura 68 • Al-‘Kalam

# Al Qalam

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. *Nun*.

Pali cholembera ndi zimene amalemba. 2. Mwachisomo
cha Ambuye wako, sindiwe wamisala ayi. 3. Ndithudi iwe
udzalandira mphotho yosatha. 4. Ndithudi iwe uli ndi
makhalidwe abwino. 5. Iwe udzaona ndipo nawo adzaona.
6. Kuti ndani wa inu amene ndi wamisala. 7. Ndithudi
Ambuye wako amadziwa bwino amene wasochera ku njira
yake ndipo amadziwa bwino amene amayenda m’njira
yoyenera.

8. Motero usatsatire zochita za anthu osakhulupirira.
9. Iwo afuna utagwirizana nawo kuti nawonso agwirizane
nawe. 10. Ndipo usamvere zonena za munthu wotukwana
amene alibe phindu. 11. Woononga mbiri ya anzake ponena

za bodza, 12. Woletsa ntchito zachilungamo, wophwanya
malamulo ndi wochita zoipa, 13. Woipa mtima ndipo
wobadwa mosalongosoka 14. Chifukwa iye ali ndi chuma
ndi ana. 15. Pamene chivumbulutso chathu chilakatulidwa
kwa iye, amati: “Ndi nkhani za anthu a makedzana.” 16. Ife
tidzaika chizindikiro pa mphuno pake.

17. Ndithudi Ife tidawayesa iwo monga momwe
tidawayesera eni ake a munda, amene adalumbira kuti
adzakolola mbewu zawo m’mawa mwake. 18. Osaonjezera
mawu oti: “Ngati Mulungu alola.” 19. Kotero kudadutsa
china chake chochokera kwa Ambuye wako nthawi ya
usiku ndi kuwotcha pamene iwo anali kugona. 20. Ndipo
m’mawa, munda udasanduka wakuda monga mdima
wa usiku. 21. Ndipo mmawa iwo adaitanizana wina ndi
mnzake. 22. Nati: “Mulawirire ku munda ngati mufuna
kukakolola.” 23. Ndipo iwo adapita, namanong’onezana
wina ndi mnzake 24. “Palibe munthu wosauka amene
adzaloledwa kulowa m’mundamo kudzapempha” 25. Ndipo
m’mawa, onse adapita ndi mphamvu zotchinjirizira anthu
osauka. 26. Koma pamene iwo adaona zimene zidachitika,
onse adati: “Ndithudi ife talakwa.” 27. “Iai! Ndithudi ife
tapwetekeka.” 28. Wangwiro amene anali pakati pawo adati:
“Kodi ine sindidakuuzeni kuti bwanji inu simunena kuti:
Ngati Mulungu alola?” 29. “Iwo adati ulemerero ukhale
kwa Ambuye wathu! Ndithudi ife ndife olakwa.” 30. Ndipo
iwo adayamba kudzudzulana kuti wina adali wolakwa.
31. Iwo adati: “Tsoka kwa ife! Ndithudi Ife tidali ophwanya
malamulo.” 32. “Mwina kuti Ambuye wathu adzatipatsa
munda wina wabwino m’malo mwa uwu. Ndithudi ndi kwa
Iye kumene timapempha modzichepetsa.” 33. Chimenechi

ndicho chilango koma ndithudi chilango cha m’moyo
umene uli nkudza ndi chowawa kwambiri, iwo akadadziwa.
34. Ndithudi anthu onse angwiro adzalandira minda
ya madalitso imene ili ndi Ambuye wawo. 35. Kodi Ife
tidzasamala anthu angwiro chimodzimodzi ndi anthu
ochimwa? 36. Kodi mwatani? Kodi inu mumaweruza bwanji?
37. Kapena kodi muli ndi Buku limene mumawerengamo
38. Kuti inu mudzapeza m’menemo chilichonse chimene
mukufuna? 39. Kapena inu mwalandira kuchokera kwa Ife,
lonjezo lotsimikizika mpaka pa tsiku louka kwa akufa kuti,
ndithudi, inu mudzapeza zimene mukufuna? 40. Tawafunsa
ngati wina wa iwo angachitire umboni za lonjezolo.
41. Kapena, kodi iwo ali ndi milungu ina? Aleke abweretse
milungu yawo ngati iwo anena zoona.
42. Ndi patsiku limene chinthu choopsa chidzachitika, iwo
adzaitanidwa kuti apembedze, koma adzalephera kutero.
43. Maso awo adzayang’ana pansi ndipo adzanyozedwa
kwambiri chifukwa iwo adauzidwa kupembedza
pamene adali pa mtendere. 44. Kotero ndisiyire aliyense
amene akutsutsana ndi chenjezo ili. Ife tidzawalanga
pang’onopang’ono m’njira imene iwo saizindikira. 45. Ndipo
Ine ndidzalekerera pa kanthawi! Ndithudi chikonzero
changa ndi champhamvu.
46. Kapena kodi iwe uli kuwafunsa malipiro moti iwo ali
ndi ngongole yambiri? 47. Kapena kodi iwo amadziwa za
Buku lobisika kuti iwo akhoza kulemba? 48. Motero pirira
podikilira chiweruzo cha Ambuye wako ndipo usakhale
ngati amene adamezedwa ndi nsomba pamene adalira
kupempha chithandizo iye ali m’mavuto. 49. Ngati Ambuye
wake akadapanda kumuonetsa chisomo chake, ndithudi iye

akadakhalabe koma iye adaponyedwa pa mtunda pamene
anali wolakwa. 50. Koma Ambuye wake adamusankha ndipo
adamuchititsa kukhala wabwino. 51. Ndipo, ndithudi, iwo
onse osakhulupirira akadakusokeretsa ndi maso awo
pamene amakumbutsidwa ndipo amati: “Ndithudi uyu ndi
Wamisala.” 52. Koma ichi si china koma chikumbutso kwa
zolengedwa zonse.

Sura 69 • Al-Ha’k’kah

# Al Haqqa

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. Choonadi chenicheni! 2. Kodi choonadi chenicheni ndi
chiyani? 3. Kodi ndi chiyani chimene chingakupangitse kuti
udziwe kuti choonadi chenicheni ndi chiti? 4. Mtundu wa
Thamoud ndi Ad adakana Ola la chionongeko. 5. Ndipo
anthu a Thamoud adaonongeka ndi mfuwu woopsya.
6. Ndipo anthu a Aad adaonongeka ndi chimphepo cha
mkuntho. 7. Chimene Mulungu adachilamulira kuti
chikunthe pa iwo usiku usanu ndi uwiri ndi usana usanu
ndi utatu mosalekeza. Moti iwe ukadawaona anthu
atagonagona ukadayesa kuti ndi mitengo ya migwalangwa
yakugwa. 8. Kodi uli kuona wina wa iwo opulumuka?
9. Ndipo Farao ndi anthu amene adalipo iye asadabadwe,
ndi a mizinda imene idaonongeka anali kuchita zoipa.
10. Ndipo iwo sanamvere Mtumwi wochokera kwa Ambuye
wawo ndipo Iye adawalanga ndi chilango chowawa zedi.

11. Ndithudi! Pamene madzi anasefukira, Ife tidakunyamulani
inu m'chombo. 12. Kuti tikhoza kuchipanga icho kukhala
chikumbutso ndi kuti khutu la kumva limve.
13. Ndipo pamene lipenga lidzaimbidwa kamodzi.
14. Ndipo nthaka ndi mapiri anyamulidwa pamodzi ndi
kuponyedwa pansi mwamphamvu kamodzi. 15. Patsiku
limeneli chinthu choopsa chidzachitika. 16. Ndipo thambo
lidzaphwanyika ndipo lidzakhala lopanda mphamvu.
17. Ndipo Angelo adzaima mbali zonse ndipo angelo asanu
ndi atatu pa tsikuli adzanyamula Mpando wa Chifumu wa
Ambuye wako. 18. Patsiku limeneli mudzaweruzidwa ndipo
palibe chinthu chachinsinsi chimene chidzabisika.
19. Ndipo yense amene adzapatsidwa Buku lake kudzanja
lamanja adzati: "Ah taonani! Werengani Buku langa!"
20. Ndithudi, ine ndidakhululupira kuti tsiku lina zochita
zanga zidzaweruzidwa. 21. Kotero iye adzakhala ndi moyo
wa chisangalalo. 22. M'munda wapamwamba. 23. Wa zipatso
zokoma zimene zili pafupi. 24. Idyani ndipo imwani mmene
mufunire chifukwa cha ntchito zanu zabwino zimene
mudatumiza patsogolo panu m'masiku apitawo. 25. Koma
iye amene adzapatsidwe buku lake m'dzanja lamanzere,
adzati: "Kukadakhala bwino ngati Buku langa likadakhala
losaperekedwa kwa ine." 26. "Ndipo sindikadziwa kuti
zochita zanga zachuluka bwanji." 27. "Ikadakhala bwino imfa
ikadangodza pa ine." 28. "Chuma changa sichidandithandize
chilichonse." 29. "Ulamuliro wanga wonse wachoka kwa
ine." 30. "Mugwireni ndipo mumumange." 31. "Ndipo
m'ponyeni M'ng'anjo ya moto." 32. "Ndipo mumangeni
ndi unyolo wotalika malipande makumi asanu ndi awiri."
33. Ndithudi, iye samakhulupirira mwa Mulungu wamkulu.

34. Ndipo sadali kuthandiza kudyetsa anthu osowa.
35. Motero lero iye sadzakhala ndi bwenzi aliyense.
36. Kapena chakudya china chilichonse kupatula zonyasa
zochoka pa zilonda. 37. Palibe amene adzachidya kupatula
ochimwa ndi osakhulupilira.
38. Motero Ine ndilumbira pali chilichonse chimene uli
nkuona. 39. Ndi chimene chili chobisika. 40. Kuti ndithudi
awa ndi mawu a Mtumwi wolemekezeka. 41. Ndipo si
mawu a Mlakatuli ayi ndipo chikhulupiriro chanu ndi
chochepa. 42. Ndipo si mawu a munthu wa maula ayi,
ndipo ndi zochepa zimene inu mukumbukira. 43. Ichi ndi
chivumbulutso chochokera kwa Ambuye wa zolengedwa
zonse. 44. Ndipo iye akanapeka nkhani yokhudza Ife.
45. Ndithudi Ife tikadagwira dzanja lake lamanja. 46. Ndipo,
ndithudi, Ife tikadadula mtsempha wake wa moyo. 47. Ndipo
palibe, wina wa inu, amene akadatiletsa Ife kumugwira.
48. Ndipo, ndithudi, Korani iyi ndi chikumbutso kwa iwo
amene amapewa zoipa. 49. Ndipo, ndithudi, Ife timadziwa
kuti alipo ena a inu amene amaikana. 50. Ndipo, ndithudi,
ilo lidzakhala lomvetsa chisoni kwa anthu osakhulupirira.
51. Ndipo, ndithudi, ichi ndi choonadi chokhachokha.
52. Motero lemekeza dzina la Ambuye wako, Wamkulu kulu.

# Al Ma'arij

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Wofunsa adafunsa za chilango chimene chichitike. 2. Pa
anthu onse osakhulupirira, chimene wina sangachiletse.
3. Kuchokera kwa Ambuye, Mwini njira zokwerera
kumwamba. 4. Angelo ndi Mzimu amakwera kupita
kwa Iye mtsiku limodzi limene lingafanizidwe ndi zaka
zikwi makumi asanu. 5. Kotero pirira kupilira kwabwino.
6. Ndithudi! Iwo amaona kuti ili patali. 7. Koma Ife tili
kuliona lili pafupi. 8. Tsiku limene kumwamba kudzaoneka
ngati mkuwa wachiphalaphala. 9. Ndipo mapiri adzakhala
ngati ubweya wouluka. 10. Ndipo palibe bwenzi amene
adzafunse za bwenzi lake. 11. Iwo azidzawaona iwo.
Munthu wochita zoipa adzafunitsitsa kuti mwina akhoza
kudzipulumutsa ku chilango cha tsikuli popereka ana ake.
12. Ndi mkazi wake ndi m'bale wake. 13. Ndi anansi ake
amene adamusunga. 14. Ndipo zonse zimene zili padziko
lapansi kuti mwina zikhoza kumupulumutsa.

15. Kosatheka! Ndithudi udzakhala moto wa lawilawi
wa ku Gahena. 16. Wotentha mutu wonse. 17. Udzaitana
aliyense amene amakana choonadi. 18. Ndipo amangopanga
chuma ndi kuchisunga. 19. Ndithudi Munthu adalengedwa
kukhala wosapirira. 20. Amakhala modandaula ngati
mavuto amupeza. 21. Ndipo amachita mwano ngati apeza
zabwino. 22. Kupatula okhawo amene amapemphera

nthawi zonse. 23. Iwo amene amapemphera mowirikiza.
24. Ndi iwo amene m'chuma chawo muli gawo limene
amasiya padera. 25. Kuti apereke kwa anthu opempha ndi
amene ali pa mavuto. 26. Ndi iwo amene amakhulupirira
kuti kudzakhala tsiku lachiweruzo. 27. Ndi iwo amene
amachita mantha ndi chilango cha Ambuye wawo.
28. Ndithudi chilango cha Ambuye ndi chosatetezeka.
29. Ndi iwo amene amadzisunga. 30. Kupatula akazi
awo ndi akapolo awo chifukwa iwo sadzadzudzulidwa.
31. Koma aliyense amene afuna kuposa awa, ndi wophwanya
malamulo. 32. Ndi iwo amene amasunga malonjezo ndi
malamulo awo. 33. Ndi iwo amene amapereka umboni
woona nthawi zonse. 34. Ndi iwo amene amalabadira
mapemphero awo. 35. Awa ndiwo amene adzalemekezeka
m'minda ya Paradiso.

36. Kodi chachitika ndi chiyani kwa anthu osakhulupirira
kuti azibwera mwaliwiro kudza kwa iwe? 37. Kuchokera
kumbali ya dzanja lamanja ndi mbali yakumanzere mu
unyinji wawo? 38. Kodi aliyense wa iwo amayembekeza
kukalowa m'munda wa chisangalalo? 39. Kosatheka!
Ndithudi Ife tawalenga kuchokera ku chinthu chimene
sachidziwa.

40. Motero, Ine ndilumbira pa Ambuye wa malo onse a
kum'mawa ndi kumadzulo kuti Ife tikhoza 41. Kuika anthu
ena abwino m'malo mwawo ndipo palibe chinthu chimene
chingatiletse kutero. 42. Motero asiye ayambe adzinyenga
ndi chisangalalo mpaka pamene adzakumana ndi tsiku
lawo limene adalonjezedwa. 43. Tsiku limene adzatuluka
mwansanga m'manda mwawo ngati anthu a pa mpikisano
umene amalandirirapo mphotho. 44. Atayang'ana maso awo

pansi ndipo adzachititsidwa manyazi. Limeneli ndilo tsiku limene analonjezedwa.

SURA 71 • NÛH

# NUH

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Ndithudi tidatumiza Nowa kwa anthu ake: "Chenjeza anthu ako chilango chowawa chisadafike pa iwo."
2. Iye adati: "Oh inu anthu anga! Ndithudi ine, ndine Mchenjezi wooneka kwa inu." 3. "Kuti muzipembedza Mulungu ndi kumuopa Iye ndipo mundimvere ine." 4. "Iye adzakukhululukirani machimo anu ndi kukusunganі bwino mpaka nthawi ya imfa yanu. Ndithudi nthawi ya Mulungu ikakwana, palibe wina aliyense amene angaibwezere m'mbuyo inu mukadadziwa." 5. Iye adati: "Oh Ambuye! Ndithudi usana ndi usiku ndakhala ndiri kuwaitana anthu anga." 6. "Koma kuitana kwanga kwangoonjezera kusamvera kwawo." 7. "Ndipo, ndithudi, nthawi yonse imene ndiitana kuti Inu muwakhululukire, iwo amatenga zala zawo ndi kutseka m'makutu mwawo ndipo amatenga mikhanjo yawo ndi kufunditsa kumutu kwawo ndipo amapitirirabe kuchita zoipa monyada." 8. "Ndipo, ndithudi, ine ndidalalikira mokweza kwa iwo." 9. "Ndipo, ndithudi, ndidawalankhula pagulu ndi mwamseri." 10. Ndidawauza: "Funsani chikhululukiro cha Ambuye wanu. Ndithudi Iye amakhululukira nthawi zonse." 11. "Iye adzakutumizirani

mvula yochuluka.” 12. “Ndikukupatsani inu chuma, ana,
minda ndi mitsinje.” 13. Kodi mwatani, inu simuyembekeza
mphotho? 14. Pamene Iye adakulengani inu m’nthawi
zosiyana siyana. 15. Kodi inu simuona mmene Mulungu
adalengera miyamba isanu ndi iwiri, wina pamwamba pa
unzake? 16. Ndipo anapanga mwezi ngati muuni ndi dzuwa
ngati nyali? 17. Mulungu adakulengani inu kuchokera ku
nthaka. 18. Ndipo ku nthaka komweko adzakubwezerani
inu ndi kukudzutsaninso. 19. Ndipo Mulungu adalenga
dziko kukhala lalikulu kwa inu. 20. Kuti muziyenda m’njira
zambiri za zikuluzikulu.

21. Nowa adati: “Oh Ambuye! Anthu anga sali
kundimvera ine koma mmalo mwake ali kutsatira amene
sangawaonjezere chuma ndi ana koma mavuto.” 22. Ndipo
iwo akonza chiwembu champhamvu. 23. Ndipo ati:
“Mwanjira ina iliyonse inu musaleke kupembedza milungu
yanu. Musaleke kupembedza Wadd, Suwa, Yaghuth, Yauq
kapena Nasr.” 24. “Ndipo, ndithudi, iwo asocheza anthu
ambiri. Ndipo Inu musaonjeze china chili chonse kwa
anthu ochita zoipa chifukwa apitirizabe kuchita zoipa.”
25. Chifukwa cha machimo awo iwo anamizidwa ndipo
adaponyedwa ku moto ndipo iwo sanapeze wina aliyense
kuti awathandize, m’malo mwa Mulungu.

26. Ndipo Nowa adati: Ambuye wanga! Musasiye munthu
aliyense padziko lapansi mwa anthu osakhulupirira.
27. “Ngati Inu muwasiya iwo adzasocheretsa akapolo anu
okhulupirira ndipo iwo adzabereka anthu ochita zoipa
ndi osakhulupirira.” 28. “Ambuye wanga! Ndikhululukireni
ine ndi makolo anga ndi iye amene alowa mnyumba
yanga ngati wokhulupirira ndiponso okhulupirira onse

amuna ndi akazi. Ndipo kwa anthu osakhulupilira, Inu musawaonjezere china koma chionongeko!

Sura 72 • Al-Jînn

## Al Jinn

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Nena: "Zavumbulutsidwa kwa ine kuti gulu la majini
lidamvera chivumbulutso cha Mulungu ndipo lidati:
Ndithudi ife tamva mawu odabwitsa." 2. "Amene apereka
dongosolo la kunjira yoyenera ndipo ife takhulupirira zonse
zimene zinali kunenedwa ndipo ife sitidzalambira wina
aliyense kupatula Ambuye wathu." 3. 'Ulemerero ukhale
kwa Ambuye wathu. Iye sadakwatire kapena kubereka
ana. 4. 'Ndipo kuti anthu opusa amene ali pakati pathu
akhala ali kumanenera Mulungu zinthu zonyasa kwambiri.
5. 'Ndipo, ndithudi, ife timaganiza kuti kulibe munthu
kapena majini amene angakanene chinthu chabodza
chokhudza Mulungu. 6. 'Ndipo, ndithudi, padali anthu
pakati pa mtundu wa anthu amene amapeza chitetezo
kuchokera kwa anthu a mtundu wa majinn. Koma iwo
adangoonjezera kuchita zoipa ndi kusakhulupilira.
7. 'Ndipo iwo adayamba kuganiza monga momwe inu
mumaganizira, kuti Mulungu sadzadzutsa wina aliyense.
8. 'Ndipo ife tidafuna kupita kuthambo la pamwamba zedi
ndipo tidaona kuti linali lodzadzidwa ndi ogwira ntchito
a mphamvu ndi nyenyezi za moto. 9. 'Ndithudi ife tinali

kukhala m'menemo kumvetsera koma amene azimvetsera
tsopano, adzapeza malawi a moto uli kumudikira. 10. 'Ife
sitidziwa ngati akuwafunira mavuto anthu awo amene ali
padziko lapansi kapena kuti Ambuye wawo ali ndi cholinga
choti awatsogolere. 11. 'Alipo ena pakati pathu amene
ndi angwiro pamene ena ndi ochimwa. Ife ndife magulu
otsatira njira zosiyanasiyana. 12. 'Ndipo ife timaganiza
kuti sitingathawe Mulungu padziko lapansi ndiponso
sitingathawe pothamangitsidwa. 13. 'Ndipo, ndithudi,
pamene tidamva ulangizi wake, ife tidakhulupirira ndipo
aliyense amene amakhulupirira mwa Ambuye wake sakhala
ndi mantha otaya zake kapena kuponderezedwa. 14. 'Ndipo
pakati pathu pali ena amene amadzipereka kwathunthu
kwa Mulungu ndi ena amene amachita zoipa. Iwo amene
adzipereka kwa Mulungu amatsatira njira yoyenera."
15. Ndipo iwo amene amachita zoipa adzakhala nkhuni za
ku Gahena.

16. Ngati iwo akanakhulupirira ndi kutsatira njira
yoyenera, Ife, ndithudi, tikadawapatsa mvula yambiri.
17. Kuti tikhoza kuwayesa ndi izo. Ndi aliyense amene
samvera chenjezo la Ambuye wake. Iye adzakonza kuti
alandire chilango chowawa zedi. 18. Ndipo Mizikiti ndi
ya Mulungu yekha. Motero musapembedze mulungu
wina pambali pa Mulungu m'modzi yekha. 19. Ndipo
pamene kapolo wa Mulungu anaima kupempha kwa Iye,
iwo adamuzungulira mu unyinji wawo mopanikizana.
20. Nena: "Ine ndimapempha kwa Ambuye wanga ndipo
sindimufanizira Iye ndi wina aliyense." 21. Nena: "Ine
ndilibe mphamvu yobweretsa pa inu chinthu choipa kapena
kukubweretsani ku njira yoyenera." 22. Nena: "Palibe wina

aliyense amene anganditeteze ine kwa Mulungu ndipo ine sindingapeze kothawira kwina kulikonse kupatula kwa Iye yekha." 23. "Udindo wanga ndi kukuuzani choonadi chimene ndalandira kuchokera kwa Mulungu ndi Uthenga wake, ndipo aliyense amene amanyoza Mulungu ndi Mtumwi wake adzakhala ku moto wa ku Gahena nthawi zonse."

24. Mpaka pamene iwo ataona kuopsa kwa chilango chimene chidalonjezedwa kuti chidzafika pa iwo, pamenepo ndipo pamene adzadziwa mbali imene wopanda mphamvu ali ndipo kuti ndi ayani amene anali wochepa m'chiwerengero. 25. Nena: "Ine sindidziwa ngati chimene mwalonjezedwa chidzafika msanga kapena kuti Ambuye wanga adachiiika patali." 26. Iye yekha ndiye amene amadziwa zonse zobisika ndipo zinsinsi zake saululira wina aliyense ayi. 27. Kupatula kwa Atumwi ake amene Iye amawasankha yekha. Ndipo Iye amatumiza gulu la Atetezi amene amayenda patsogolo ndi pambuyo pawo. 28. Amawateteza mpaka pamene aona kuti iwo apereka uthenga wochokera kwa Ambuye wawo. Ndipo Iye amadziwa chili chonse chimene ali nacho ndipo Iye amasunga chiwerengero cha chinthu chili chonse.

# Al Muzzammil

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Oh iwe amene wadzikulunga m'chovala! 2. Dzuka usiku
onse kupatula kwanthawi kochepa. 3. Theka la usikuwo
kapena kanthawi kocheperako. 4. Kapena kwa kanthawi
kochulukirapo ndipo lakatula Korani modekha ndi
modukizadukiza monga mmene umayenera kuchitikira.
5. Ndithudi, Ife tidzakutumizira Mawu a mphamvu.
6. Ndithudi kuuka nthawi ya usiku ndi kovuta, ndipo
mau amatchulidwa bwino. 7. Ndithudi, iwe masana
umatangwanika kwambiri. 8. Ndipo uzikumbukira dzina
la Ambuye wako ndipo udzipereke kwathunthu kwa Iye.
9. Iye ndiye Ambuye wa kum'mawa ndi wa kumadzulo.
Kulibe Mulungu wina koma Iye yekha. Mulandire Iye
kuti akhale Mtetezi wako. 10. Pirira pa zonse zimene
ali kunena ndipo siyana nawo mwaulemu. 11. Undisiyire
Ine onse amene amakana choonadi nthawi zonse ndipo
pirira ndi iwo pakanthawi kochepa. 12. Ife, ndithudi, tili
ndi unyolo ndipo tawasungira moto wosatha kuuzima.
13. Ndi chakudya chotsamwitsa ndi chilango chowawa.
14. Patsiku limene dziko ndi mapiri zidzagwedezeka
kwambiri ndipo mapiri adzakhala mulu wa mchenga
wotaika umene umatuluka kupansi.
15. Ndithudi Ife tatumiza Mtumwi kukhala umboni
wokutsutsani monga momwe tidatumizira Mtumwi

kwa Farao. 16. Koma Farao sadamumvere Mtumwi
ndipo Ife tidamulanga ndi chilango choopsa. 17. Kodi
ngati inu simukhulupirira, mudzalithawa bwanji tsiku
limene lidzachititsa ana anu a ang'ono kukhala ndi imvi?
18. Tsiku limene thambo la kumwamba lidzang'ambika
pakati. Ndithudi lonjezo la Mulungu lidzakwaniritsidwa.
19. Ndithudi ili ndi chenjezo chabe, motero musiyeni
aliyense amene afuna kuti atsatire njira yoyenera yonka
kwa Ambuye wake kuti aitsatire.

20. Ndithudi Ambuye wako amadziwa kuti nthawi zina iwe
umakhala tcheru mphindi ziwiri pakati pa mphindi zitatu
za usiku, mwina theka la usiku ndipo nthawi zina mphindi
imodzi pakati pa mphindi zitatu za usiku, monga momwe
gulu lina la anthu amene ali nawe. Ndipo Mulungu ndiye
amene amasiyanitsa usiku ndi usana. Iye amadziwa kuti
siungathe kupemphera mphindi zonse ndipo wakuyang'ana
mwachisoni. Kotero lakatula magawo ena a Korani amene
angakhale apafupi kwa iwe. Iye amadziwa kuti pakati panu
pali anthu odwala ndi ena amene ali kupita uku ndi uku
padziko kufunafuna zokoma za Mulungu ndi ena amene ali
kumenya nkhondo m'njira ya Mulungu. Motero lakatula,
mawu a m'Korani, amene ungathe kulakatula, ndipo
pitiriza kupemphera ndipo pereka msonkho wothandiza
anthu osauka ndipo kongoza ngongole yabwino kwa
Mulungu ndipo chabwino chilichonse chimene muli
kutsogoza, mudzachipeza kwa Mulungu, chitasungidwa
bwino ndipo mudzalandira mphotho ya mtengo wapatali
kuchokera kwa Iye. Ndipo pempha chikhululukiro kwa
Mulungu. Ndithudi Mulungu ndi wokhululukira ndi wa
chisoni chosatha.

# AL MUDDATHTHIR

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Oh iwe amene wakutidwa! 2. Dzuka ndi kupereka chenjezo!
3. Ndipo lemekeza Ambuye wako! 4. Ndipo yeretsa zovala
zako. 5. Ndipo pewa zonse za mafano. 6. Ndipo usapereke
thandizo ndi cholinga chopezamo cholowa. 7. Ndipo khala
wopirira chifukwa cha Ambuye wako.
8. Ndipo pamene lipenga lidzalira. 9. Ndithudi limeneli
lidzakhala tsiku loopsa. 10. Tsiku lamavuto kwa anthu onse
osakhulupirira. 11. Ndisiye ndekha kuthana ndi munthu
amene ndidamulenga ndekha. 12. Ndipo ndidamupatsa
chuma chosawerengeka. 13. Ndi ana okhala pambali pake.
14. Ndipo Ine ndidamuchitira zonse kuti zikhale
zolongosoka ndi zapafupi. 15. Koma nthawi zonse amafuna
kuti ndizimupatsabe zinthu zambiri. 16. Kosatheka!
Ndithudi iye wakhala ali kuchitira mwano chivumbulutso
chathu. 17. Ine ndidzamukhaulitsa pomupatsa chilango
chowawa.
18. Ndithudi iye adaganiza ndipo adakonza chiwembu.
19. Ndipo ayenera kutembererewa chifukwa cha chiwembu
chake. 20. Motero iye ayenera kutemberedwa chifukwa
cha chiwembu chake. 21. Ndipo iye anayang'ana. 22. Ndipo
iye adachita matsinya ndipo anaonetsa kuipidwa. 23. Kenaka
adatembenukira kumbali modzikweza. 24. Ndipo iye adati:

“Ichi sichina koma matsenga a anthu a amakedzana!”
25. “Ichi sichina koma mawu a munthu chabe.”
26. Ine ndidzamuponya iye ku Gahena. 27. Kodi
chidzakudziwitsa kuti moto wa ku Gahena ndi chiani?
28. Iwo susunga kapena kusiya. 29. Umatentha matupi.
30. Umasamalidwa ndi angelo khumi ndi asanu ndi anayi. 31. Ife
sitidasankhe wina aliyense koma angelo kuti aziyang’anira
moto ndipo tinakhazikitsa chiwerengero chawo ngati
mayesero kwa anthu osakhulupirira, kuti iwo onse amene
alandira mawu a Mulungu akhulupirire ndi kuti anthu
okhulupirira m’choonadi apitirize chikhulupiriro chawo;
kuti iwo amene adalandira kale mawu a Mulungu ndiponso
anthu onse okhulupirira moona asakhale ndi chikaiko
china chilichonse; ndipo kuti onse amene m’mitima
mwawo muli matenda pamodzi ndi anthu osakhulupirira
anganene kuti: “Kodi Mulungu afuna kutanthauza chiyani
pa chitsanzo chotere?” Mmenemo ndi mmene Mulungu
amasokeretsera munthu aliyense amene Iye wamufuna ndi
kutsogolera aliyense amene Iye wamufuna. Palibe munthu
amene amadziwa asirikali a Ambuye wako kupatula Iye
mwini. Ichi si china chilichonse koma chikumbutso kwa
anthu onse.
32. Iyayi, ndilumbira pali mwezi. 33. Ndi pali usiku pamene
uli n’kutha. 34. Ndi pali m’mbandakucha pamene uli
n’kudza. 35. Ndithudi ili ndi limodzi la masoka akuluakulu.
36. Ndi chenjezo kwa anthu onse. 37. Kwa yense wa inu
amene afuna kupitirirabe mtsogolo kapena afuna kutsalira
m’mbuyo. 38. Munthu aliyense adzafunsidwa molingana ndi
ntchito zake. 39. Kupatula iwo amene adzakhala kudzanja
lamanja. 40. M’minda, iwo azidzafunsana wina ndi mnzake.

41. Za anthu ochimwa kuti: 42. Kodi ndi chiyani chimene
chakulowetsani inu ku moto? 43. Iwo adzayankha nati: “Ife
sitimapemphera.” 44. Ndiponso sitimadyetsa anthu a njala.
45. Ife timangotsutsa zinthu mwaumbuli. 46. Ndipo tidali
kunena kuti kulibe tsiku lachiweruzo. 47. Mpaka pamene
imfa idatipeza. 48. Motero palibe chidandaulo chochokera
kwa wina aliyense chimene chidzamveka.

49. Kodi ndi chifukwa chiyani iwo ali kuthawa chikumbutso
ichi? 50. Monga abulu odzidzimutsidwa. 51. Omwe anali
kuthawa Mlenje, Mkango kapena nyama ina yoopsya.
52. Iai! Aliyense wa iwo afuna kuti apatsidwe masamba
a Buku otambasula. 53. Ndikosatheka! Koma iwo alibe
mantha ndi zimene zili nkudza. 54. Iyayi. Ndithudi ili ndi
chenjezo. 55. Motero musiyeni amene afuna kuti awerenge
ndi kulandira chenjezo. 56. Ndipo iwo sadzalandira chenjezo
pokha pokha ngati Mulungu afuna. Iye ndiye Ambuye
wofunika kuti anthu onse azichita mantha ndi Iye, ndipo
Iye ndi Ambuye wokhululukira.

Sura 75 • Al-'Kiyâmah

# Qiyamah

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ine ndilumbira pali tsiku lachiweruzo 2. Ndipo ndilumbira
pali munthu amene amadzidzudzula yekha 3. Kodi munthu
amaganiza kuti Ife sitidzalumikiza mafupa ake? 4. Inde
Ife tikhoza kulumikiza mwaubwino nsonga za zala zake.

5. Ngakhale tero, munthu amafuna kupitiliza kuchita
zoipa. 6. Iye amafunsa: "Kodi zimenezi zidzachitika
liti?" 7. Motero pamene maso adzathodwa. 8. Ndipo
pamene mwezi udetsedwa. 9. Pamene dzuwa ndi mwezi
zidzakumana. 10. Patsikuli munthu adzafunsa kuti: "Kodi
ndithawira kuti tsopano?" 11. Iai! Kulibe malo othawirako!
12. Ndi kwa Ambuye wako kokha kumene kudzakhala
kothawira. 13. Patsiku limeneli, munthu adzauzidwa zonse
zimene adachita kuyambira poyamba mpaka pomaliza.
14. Iai! Munthu adzadzichitira umboni wodzineneza yekha.
15. Ngakhale kuti iye azidzayesa kudzipulumutsa yekha.

16. Usagwedeze lilime lako zokhudza Korani ponena
mofulumira. 17. Ndi udindo wathu kuisonkhanitsa ndi
kukupatsa nzeru kuilakatula iyo. 18. Ndipo pamene
talakatula, tsatira mwandondomeko kalakatulidwe kake.
19. Ndi udindo wathu kukufotokozera tanthauzo lake.

20. Iyayi! Koma inu mukonda moyo wotha msanga. 21. Ndipo
simufuna kulabadira za moyo umene uli nkudza. 22. Nkhope
zina, pa tsiku limeneli, zidzakhala zowala ndi chisangalalo.
23. Zili kuyang'ana kwa Ambuye wawo. 24. Ndipo nkhope
zina, patsiku limeneli, zidzakhala zachisoni. 25. Pozindikira
kuti chilango chowawa chidzagwa pa iwo. 26. Iyayi, pamene
ufika mpaka pa khosi. 27. Ndipo kudzanenedwa kuti: "Kodi
palibe woti angamuchize ndi kumupulumutsa ku imfa?"
28. Ndipo iye adzadziwa kuti awa ndi mathero a moyo wake.
29. Ndipo mwendo udzatembenuzika pa unzake. 30. Tsiku
limeneli zonse zidzabwerera kwa Ambuye wako.

31. Iye sanali kuvomereza chilungamo kapena
kupemphera. 32. Koma m'malo mwake adakana choonadi
ndi kubwerera m'mbuyo! 33. Ndipo iye anapita kubanja

lake monyada ali kudziyamikila yekha! 34. Tsoka kwa iwe.
Ndiponso tsoka kwa iwe! 35. Kachiwiri tsoka lili pafupi ndi
iwe, tsopano tsoka lili pafupi. 36. Kodi munthu amaganiza
kuti tidzangomulekerera kuti azichita chilichonse chimene
afuna? 37. Kodi iye sanali dontho la umuna limene lidatuluka?
38. Ndipo iye adakhala kam'bulu ka magazi. Ndipo Mulungu
adamuumba ndipo adamukonza m'maonekedwe okongola.
39. Ndipo adamulenga m'mitundu iwiri, mwamuna ndi
mkazi. 40. Kodi Iye alibe mphamvu yopereka moyo kwa
anthu akufa?

SURA 76 • AL-INSÂN

# AL INSAN

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Kodi sipadali nthawi imene munthu sanali kanthu kena
kali konse kodziwika? 2. Ndithudi Ife tidamulenga munthu
kuchokera ku madontho a umuna umene unasakanizidwa
ndi ukazi ndi cholinga chomuyesa motero Ife tidamupanga
iye kukhala wakumva ndi woona. 3. Ndithudi Ife
tamulangiza njira yabwino kaya iye akhala wothokoza
kapena wosathokoza.

4. Ndithudi tawakonzera anthu osakhulupirira unyolo
ndi magoli ndi moto wa lawilawi. 5. Ndithudi anthu
onse angwiro adzamwa chakumwa chosakanizidwa ndi
madzi ochokera pa kasupe wa ku Paradiso chotchedwa
Kafur. 6. Kasupe amene akapolo a Mulungu adzamwapo,

amene amatumphutsa madzi ochuluka. 7. Iwo amene
amakwaniritsa malonjezo awo ndipo amakhala ndi mantha
ndi tsiku limene zoipa zidzasefukira ponseponse. 8. Ndipo
amapereka chakudya chifukwa cha chikondi cha Mulungu,
kwa anthu aumphawi, amasiye ndi kwa akaidi. 9. Ife tili
kukudyetsani chifukwa cha Mulungu basi. Ife sitifuna
malipiro kapena mayamiko kuchokera kwa inu. 10. Ndithudi
ife tiopa tsiku loopsa ndi laululu limene lidzasanduliza
nkhope kuoneka monyasa, limene lili nkudza kuchokera
kwa Ambuye wathu. 11. Motero Mulungu awapulumutsa iwo
ku zoipa za tsiku limeneli ndi kuwapatsa nyali yokongola
kuti akhale mosavutika ndi mwachisangalalo. 12. Ndipo
mphotho yawo idzakhala munda wa Paradiso ndi zovala za
silika chifukwa chopirira kwawo. 13. Ali kukhala m'Paradiso,
pamipando yawofowofo, iwo sadzamva kutentha kwa
dzuwa kapena kuzizira kwambiri. 14. Ndipo mithunzi
idzakhala pafupi ndi iwo ndipo zipatso zidzalendewera
mu matsanzi kuti asamavutike pothyola. 15. Ndipo pakati
pawo padzaperekedwa zikho zozungulira za siliva ndi
matambula a magalasi. 16. Matambula oonetsa zinthu
zomwe zili m'kati mwake, opangidwa kuchokera ku siliva.
Iwo adzathiramo chakumwa molingana ndi chilakolako
chawo. 17. Ndipo iwo adzapatsidwa chakumwa kuchokera
mu zikho zodzala ndi madzi osakaniza ndi Zanjabil.
18. Kasupe amene ali komweko wotchedwa Salsabil.
19. Ndipo adzazunguliridwa ndi ana owatumikira a misinkhu
yofanana. Ndipo ngati iwe utawaona ukhoza kuganiza kuti
ndi ndolo zomwazikamwazika. 20. Ndipo pamene iwe uona
kumeneko, udzaona madalitso ndi ufumu waukulu. 21. Iwo
adzavala nsalu zokongola za silika zooneka ngati msipu

zopetedwa ndi golide. Iwo adzavala zibangiri za siliva
ndipo Ambuye wawo adzawapatsa chakumwa chabwino.
22. Ndithudi iyi ndi mphotho yanu ndipo kupirira kwanu
kwalandiridwa.

23. Ndithudi ndife amene tavumbulutsa kwa iwe pang'ono
pang'ono, Buku lolemekezeka la Korani. 24. Motero pirira
ndipo tsatira malamulo a Ambuye wako ndipo usamvere
zonena za munthu wochimwa kapena wosakhulupirira
amene ali pakati pawo. 25. Ndipo uzilemekeza dzina la
Ambuye wako m'mawa ndi madzulo. 26. Ndi m'gawo lina
la usiku, uzimupembedza Iye ndipo uzimulemekeza Iye
usiku wonse. 27. Ndithudi! Awa amakonda kwambiri moyo
wa msanga msanga wa masiku ano, ndipo amaiwala tsiku
limene lidzakhala lovuta. 28. Ndife amene tidawalenga ndipo
tinaika mphamvu m'ziwalo zawo. Koma ngati Ife titafuna,
tikhoza kulenga anthu ena kuti alowe m'malo mwawo.
29. Ndithudi! Ili ndi chenjezo motero aliyense amene afuna,
mulekeni kuti atsatire njira yoyenera yopita kwa Ambuye
wake. 30. Koma inu simudzatha kutero pokhapokha ndi
chifuniro cha Mulungu. Ndithudi Mulungu ndiye Mwini
kudziwa ndi Mwini nzeru. 31. Iye adzaonetsa chisomo chake
kwa aliyense amene Iye wamufuna. Koma anthu ochimwa,
Iye wawakonzera iwo chilango chowawa.

# Al Mursalat

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. Pali mphepo imene imatsatana pafupipafupi. 2. Pali
mphepo ya mkuntho. 3. Pali mphepo imene imamwaza
mitambo ndi mvula. 4. Pali mavesi amene amasiyanitsa
chabwino. 5. Pali angelo amene amabweretsa chivumbulutso
kwa Atumwi. 6. Kuthetsa kukangana kapena kuwachenjeza.
7. Ndithudi zonse zimene mwalonjezedwa zidzachitika.
8. Pamene nyenyezi zidetsedwa. 9. Ndi pamene thambo
la kumwamba ling'ambika pakati. 10. Ndi pamene mapiri
aphwanyika kukhala fumbi. 11. Ndi pamene Atumwi onse
asonkhanitsidwa kukhala pamalo amodzi. 12. Kodi ndi tsiku
liti limene izi zidzachitike? 13. Lidzakhala tsiku la chiweruzo.
14. Kodi ndi chiyani chidzakudziwitse za tsiku la chiweruzo?
15. Tsoka pa tsiku limeneli kwa anthu osakhulupirira! 16. Kodi
Ife sitinaononge anthu a makedzana? 17. Kotero tidzaipanga
mibadwo yotsatira kuti ione zomwezo. 18. Mmenemu ndi
mmene timakhaulitsira anthu ochita zoipa. 19. Tsoka pa
tsikuli kwa anthu osakhulupirira.
20. Kodi sitidakulengeni inu kuchokera ku madzi
onyozeka? 21. Amene tidasunga pamalo okhazikika?
22. Mpaka nthawi yake itakwana. 23. Motero Ife tinayesa
ndipo Ife wodziwa kuyesa. 24. Tsoka pa tsikuli kwa anthu
osakhulupirira. 25. Kodi Ife sitinapange nthaka ngati malo
okumaniranamo? 26. Amoyo ndi akufa, 27. Ndipo tidalenga

mapiri atali pa dziko ndi kukupatsani madzi okoma kuti
muzimwa? 28. Tsoka pa tsikuli kwa anthu osakhulupirira.
29. (Zidzanenedwa kuti): “Pitani ku chilango chimene
munkati sichidzabwera!” 30. Pitani inu mu chithunzi,
mu magulu atatu. 31. Opanda mthunzi kapena pokhala
pokutetezani ku malawi a moto. 32. Ndithudi! Umatulutsa
malawi ake akulu akulu ngati nyumba zachifumu.
33. Ndipo ooneka ngati ngamira ya chikasu. 34. Tsoka pa
tsiku limeneli kwa anthu osakhulupirira. 35. Patsiku limeneli
iwo sadzatha kulankhula. 36. Ndipo sadzaloledwa kuti
apereke chidandaulo. 37. Tsoka pa tsiku limeneli kwa anthu
osakhulupirira. 38. Limeneli ndilo tsiku la chiweruzo. Ife
takusonkhanitsani nonse pamodzi ndi anthu a makedzana.
39. Tsopano ngati inu muli ndi chiwembu, chitani chiwembu
chanu kwa Ine. 40. Tsoka pa tsiku limeneli kwa anthu
osakhulupirira.
41. Ndithudi anthu angwiro adzakhala mu mthunzi
wozizira ndi pa akasupe. 42. Ndi zipatso zimene afuna
kukhosi kwawo. 43. Idyani ndipo imwani mosangalala
chifukwa cha zimene mudachita. 44. Ndithudi, mmenemo
ndi mmene timalipirira anthu angwiro 45. Tsoka pa tsikuli
kwa anthu osakhulupirira. 46. Idyani ndipo musangalale
kwa kanthawi kochepa. Ndithudi inu ndinu oipa kwambiri.
47. Tsoka pa tsikuli kwa anthu osakhulupirira. 48. Ndipo
zikanenedwa kwa iwo kuti: “Weramani.” Iwo amakana
kutero. 49. Tsoka pa tsikuli kwa anthu osakhulupirira.
50. Kodi ndi Uthenga uti woposa uwu umene
adzaukhulupirire?

# AL-NABA

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Kodi akufunsana nkhani zotani? 2. Ali kufunsana za
nkhani ija yaikulu. 3. Nkhani imene akusiyana maganizo
pakati pawo. 4. Iyayi, iwo adzadziwa posachedwa. 5. Iyayi,
iwo adzadziwa posachedwapa. 6. Kodi Ife sitidapange
dziko lapansi monga ngati kama. 7. Ndi mapiri ngati
zikhomo. 8. Ndipo Ife tidakulengani inu awiri awiri.
9. Ndipo tidapanga tulo kukhala ngati mpumulo wanu.
10. Ndipo tidapanga usiku kukhala chophimba. 11. Ndipo
tinapanga usana kukhala kopezera zofuna zanu. 12.
Ndipo tidamanga mlengalenga miyamba isanu ndi iwiri.
13. Ndipo tidakhazikitsa mmenemo nyali yowala, 14. Ndipo
tidatumiza mvula yambiri kuchokera ku mitambo ya
mvula. 15. Kuti timeretse chakudya ndi mbewu. 16. Ndipo
minda ya zomera zothinana. 17. Ndithudi tsiku la chiweruzo
lidakhazikitsidwa kale.

18. Tsiku limene lipenga lidzalira ndipo inu mudzadza mu
magulumagulu. 19. Ndipo mu mlengalenga mudzatsegulidwa
ndipo mudzakhala ngati makomo. 20. Ndipo mapiri onse
adzayendetsedwa ndi kukhala ngati nthunzi yamadzi.
21. Ndithudi Gahena ili kuwayembekezera. 22. Mudzi wa
anthu ophwanya malamulo. 23. Kumeneko ndiko kumene
adzakhale mpaka kalekale. 24. Kumeneko sadzalawa
chozizira kapena kumwa china chilichonse. 25. Kupatula

madzi owira ndi mafinya. 26. Mphotho yoyeneradi.
27. Chifukwa, ndithudi, iwo sanali kuopa chidzudzulo
chathu. 28. Ndipo iwo moyerekedwa anali kukana
chivumbulutso chathu.

29. Ndipo Ife tidalemba m'Buku zonse zimene anali
kuchita. 30. Motero inu lawani! Inu simudzalandira china
chilichonse koma manzunzo ochuluka! 31. Ndithudi kwa
anthu oopa Mulungu kudzakhala kupambana. 32. Minda
ndi m'minda ya mphesa. 33. Ndi a namwali akulu akulu
ofanana zaka. 34. Ndi chikho chodzadza. 35. Kumeneko
iwo sadzamva mawu opanda pake kapena nkhani zabodza.
36. Imeneyi ndiyo mphotho yochokera kwa Ambuye wako
ndipo ndi mphotho yokwanira. 37. Ambuye wa Kumwamba
ndi dziko lapansi ndi zonse zimene zili pakati pawo, Mwini
chisoni chosatha ndipo iwo sadzatha kulankhula naye.
38. Patsiku limene Mzimu ndi angelo adzaima pa mizere
ndipo palibe amene adzalankhula kupatula yekhayo amene
adzalandira chilolezo cha Mwini chifundo chosatha ndipo
adzanena chinthu chimene chili choona. 39. Ndithudi tsiku
limeneli ndi loona, motero iye amene afuna, mulekeni
atsatire njira yobwerera kwa Ambuye wake. 40. Ndithudi
takuchenjezani za chilango chowawa chimene chili nkudza
posachedwa. Tsiku limene munthu adzayang'ana ntchito
zimene manja ake adatsogoza, ndipo osakhulupirira adzati:
"Kalanga ine, ndikanakhala dothi."

# AL-NAZIAT

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pali iwo amene amalanda mwankhanza. 2. Ndi pali
iwo amene amachotsa mwaufulu. 3. Ndi pali iwo amene
amauluka. 4. Ndi pali iwo amene amathamanga ngati ali
pa liwiro loopsya. 5. Ndi pali angelo amene amakwaniritsa
kuchita malamulo a Ambuye wawo. 6. Patsiku limene dziko
ndi mapiri zidzagwedezeka kwambiri. 7. Ndi kulira kwa
lipenga kawiri. 8. Mitima, patsiku limeneli, idzafumuka
ndi kuda nkhawa. 9. Maso awo atagwetsa pansi. 10. Iwo
amanena kuti: "Kodi ife tidzabwerera monga momwe
tinali poyamba?" 11. "Angakhale mafupa athu ataola?" 12. Iwo
amati: "Kubwerera kotero ndi kopanda phindu." 13. Koma
udzakhala mfuwu umodzi okha. 14. Pamene, taona, iwo
adzadzipeza okha ali pamwamba pa nthaka ali ndi moyo.
15. Kodi inu mudaimva nkhani ya Mose? 16. Pamene Ambuye
wake adamuitana mu dambo lodalitsika la Tuwa. 17. "Pita
kwa Farao; Ndithudi iye waphwanya malamulo mopyola
muyezo." 18. "Ndipo ukamuuze kuti: Kodi ungadziyeretse
wekha?" 19. "Ndi kuti ine ndikulondolere kwa Ambuye
wako kuti uzimuopa Iye?" 20. Kotero iye adamuonetsa
chizindikiro cha chikulu. 21. Koma iye adachikana ndipo
sanamvere. 22. Iye adapitirizabe kuchita zoipa. 23. Ndipo
iye adaitana anthu ake onse ndipo anafuula mokweza:
24. Nati: "Ine ndine Ambuye wanu wapamwamba mwamba."

25. Motero Mulungu adamugwetsera iye chilango chifukwa
cha mau ake omaliza ndi oyamba. 26. Ndithudi mu izi muli
phunziro lomveka kwa anthu oopa Mulungu.

27. Kodi inu ndinu ovuta kulenga kapena thambo la
mlengalenga limene Mulungu adalilenga? 28. Iye analikweza
m'mwamba ndi kulikonza bwino! 29. Usiku wake amaukuta
ndi m'dima ndipo masana ake amatulutsa kuwala. 30. Ndipo
pambuyo pake adalikulitsa dziko. 31. Ndipo anatulutsa
madzi ndi msipu. 32. Ndipo adazika mapiri molimbika.
33. Chakudya cha phindu kwa inu ndi kwa zoweta zanu.

34. Koma pamene mavuto akulu akudza. 35. Tsiku limene
munthu adzayamba kuganiza ntchito zake zonse. 36. Ndipo
Gahena idzabweretsedwa pafupi kuti aliyense aione.
37. Ndipo kwa iye ophwanya malamulo. 38. Ndipo anasankha
moyo wapadziko lino. 39. Ndithudi malo ake okhala ndi ku
Gahena. 40. Koma kwa iwo amene amaopa kukaima pamaso
pa Ambuye wake ndi machimo ndipo anali kudziletsa
kuchita chifuniro chopanda pake. 41. Ndithudi adzakhala
ku Paradiso. 42. Amakufunsa za nthawi imene chigumula
chidzabwere. 43. Iwe siudziwa zoti unene china chili chonse.
44. Ndi Ambuye wako yekha amene amadziwa tsiku. 45. Iwe
ndiwe mchenjezi chabe kwa iwo amene ali kuliopa tsikuli.
46. Patsiku limene iwo adzachiona chigumula, kudzakhala
ngati kuti iwo sanakhale padziko lapansi nthawi yaitali
koma usiku umodzi kapena usana wokha.

# Abasa

Mdzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. Iye anachita matsinya ndi kuyang'ana kumbali.
2. Chifukwa munthu wakhungu anadza kwa iye. 3. Ndipo iwe
ungadziwe bwanji kuti mwina angadziyeretse. 4. Kapena iye
adzalandira chenjezo ndipo chenjezo likanamupindulira
kanthu kena. 5. Koma iye amene amadziyesa kuti sasowa
kanthu. 6. Ameneyo ndiye amene uli naye ndi chidwi.
7. Kodi uli nazo chiani ngati iye sadziyeretsa? 8. Koma
kwa iye amene amakuthamangira. 9. Ndipo iye amaopa.
10. Iwe siudamulabadire ayi. 11. Iyayi! Ndithudi chimenechi
ndi chikumbutso. 12. Muloleni aliyense amene afuna kuti
achilabadire. 13. Ichi chidalembedwa m'Buku la Mulungu
lolemekezeka. 14. Loyeretsedwa ndi losungidwa bwino
ndi loyera. 15. M'manja mwa Alembi. 16. Wolemekezeka
ndipo womvera. 17. Atembereredwe munthu! Kodi ndi
chiani chili kumuletsa kuthokoza? 18. Kodi Iye adamulenga
kuchokera ku chiyani? 19. Kuchokera ku dontho la umuna,
Iye adamulenga ndipo adamukonza bwino. 20. Ndipo Iye
adamukonzera iye njira yapafupi. 21. Ndipo amamupha
ndi kumusunga m'manda. 22. Ndithudi Iye adzamudzutsa
monga momwe afunira. 23. Iyayi, koma munthu sanachite
zimene Iye adamulamulira. 24. Mulekeni munthu kuti
aganize za chakudya chake. 25. Kuti Ife timagwetsa mvula
yambiri. 26. Ndipo timaphwanya nthaka . 27. Ndipo Ife

timameretsa njere. 28. Mphesa ndi Msipu. 29. Mitengo ya
mafuta, ndi mitengo ya tende. 30. Ndi minda imene ili ndi
mitengo yambiri. 31. Ndi mitengo ya zipatso ndi msipu.
32. Chakudya cha inu ndi ziweto zanu. 33. Koma pamene
kulira kogonthetsa mkhutu kudzamveka. 34. Patsiku limene
munthu adzakana m'bale wake. 35. Amai ake ndi bambo ake.
36. Mkazi wake ndi ana ake. 37. Chifukwa aliyense patsiku
limeneli, adzakhala otangwanika ndi mavuto ake. 38. Patsiku
limeneli padzakhala nkhope zambiri zowala. 39. Zosekerera
ndi zachimwemwe chifukwa cha nkhani yabwino.
40. Ndipo pa tsikuli padzakhala nkhope zina zokutidwa ndi
fumbi. 41. M'dima udzakuta iwo. 42. Awa adzakhala anthu
osakhulupirira ndi ochita zoipa.

Sura 81 • At-Takwir

## Al-Takwir

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pamene dzuwa lidzavundikiridwa. 2. Ndi pamene nyenyezi
zidzagwa pansi. 3. Ndi pamene mapiri adzachotsedwa.
4. Ndi pamene ngamila zabele zizakhala zosasamalidwa.
5. Ndi nyama za m'tchire zidzasonkhanitsidwa pamodzi.
6. Ndi pamene nyanja zidzayatsidwa moto kapena
zidzasefukira. 7. Ndi pamene mizimu idzakumanitsidwa ndi
matupi awo. 8. Ndi pamene mwana wa mkazi wa mng'ono,
amene adaundilidwa wa moyo adzafunsidwa. 9. Chifukwa
chimene anamuphera. 10. Ndi pamene mabuku olembamo

ntchito za munthu aliyense adzatulutsidwa. 11. Ndi pamene
kumwamba kudzafafanizidwa ndi kuchotsedwa ku malo
ake. 12. Ndi pamene Gahena idzatenthetsedwa kwambiri.
13. Ndi pamene Paradiso idzafikitsidwa pafupi. 14. Ndithudi
munthu aliyense adzadziwa chimene adachita.

15. Motero, ndithudi, Ine ndili kulumbira pali nyenyezi
zimene zimalowa. 16. Ndi pali maiko zimene zimayenda
mofulumira ndi kudzibisa okha. 17. Ndi pali usiku pamene
uchoka. 18. Ndi pali m'mawa pamene kuli kucha. 19. Ndithudi
awa ndi Mau a Mtumwi wolemekezeka. 20. Mwini mphamvu
amene amalemekezedwa ndi Ambuye, Mwini Mpando wa
Chifumu. 21. Amamveredwa ndi wokhulupirika. 22. Ndipo
m'bale wanu uyu si wa misala ayi. 23. Ndipo, ndithudi,
iye adamuona iye mu mlengalenga. 24. Iye sabisa zinthu
zosaoneka. 25. Ndipo zimene alankhula sizochokera kwa
Satana wotembereredwa. 26. Kodi inu muli kupita kuti?
27. Ndithudi ichi si china chilichonse ayi koma chikumbutso
kwa anthu a mitundu yonse. 28. Kwa aliyense wa inu amene
afuna kuyenda moongoka. 29. Koma inu simungathe kutero
pokhapokha ndi chifuniro cha Mulungu, Ambuye wa
zolengedwe zonse.

# Infitar

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pamene thambo lidzang'ambika. 2. Pamene nyenyezi
zidzagwa ndi kubalalitsidwa. 3. Ndi pamene nyanja
zikuluzikulu zidzaphulika. 4. Pamene manda adzatseguka.
5. Pamenepo Mzimu uliwonse udzadziwa chimene
udatumiza ndi chimene udasiya m'mbuyo. 6. Oh Iwe
munthu! Kodi ndi chiyani chikukunamiza kuti usiye
kutsatira malamulo a Ambuye wako Wolemekezeka.
7. Amene adakulenga iwe ndi kukukonza kuti uzioneka
bwino monga mmene uonekeramu? 8. Ndi nkhope ina
iliyonse imene idamukondweretsa anakulenga iwe. 9. Iyayi!
Koma inu mukukana kuti kudzakhala tsiku lachiweruzo.
10. Koma pakati panu pali ena amene ali kukuyang'anirani.
11. Olemekezeka ndi odziwa kulemba. 12. Iwo amadziwa
chilichonse chimene mumachita. 13. Ndithudi anthu onse
angwiro adzakhala mu mtendere. 14. Ndipo, ndithudi,
anthu onse oipa adzakhala ku Gahena. 15. Imene iwo
adzalowako ndi kulawa malawi ake patsiku lachiweruzo.
16. Iwo sadzatha kuthawa ayi. 17. Kodi chidzakuuza ndi
chiani za tsiku lachiweruzo? 18. Tinenanso kodi chidzakuuza
ndi chiani za tsiku lachiweruzo? 19. Ndi tsiku limene
mzimu uliwonse sudzatha kuthandiza wina aliyense ndipo
Mulungu yekha ndiye amene adzaweruza.

# Al Mutaffifin

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi mwini
Chisoni Chosatha.

1. Tsoka kwa iwo onse amene amagulitsa malonda awo
monyenga. 2. Iwo amene amati ena akamawayesera zinthu
amafuna kuti zikwanire muyeso wake. 3. Koma pamene
iwo ayesa kapena awayesera anthu ena amawanyenga.
4. Kodi iwo saganiza kuti adzaukitsidwa kwa akufa.?
5. Patsiku lalikulu. 6. Tsiku limene anthu a mitundu yonse
adzaima pamaso pa Ambuye wa zolengedwa zonse. 7. Iyayi!
Ndithudi chiwerengero cha anthu onse oipa chili mu Sijjin.
8. Kodi udzadziwa bwanji Sijjin ndi chiyani? 9. Ili ndi Buku
lolembedwa. 10. Tsoka pa tsikuli kwa anthu osakhulupirira.
11. Iwo amene amakana kuti kuli tsiku lachiweruzo?
12. Palibe wina amene amalikana tsikuli kupatula munthu
wogona m'machimo. 13. Pamene chivumbulutso chathu
chinenedwa kwa iye, iye amati: "Izi ndizo nthano za anthu
akale." 14. Iyayi! Koma m'mitima mwawo ndi mokutidwa
ndi zintchito zimene amachita. 15. Iyayi! Ndithudi iwo
sadzaloledwa kuona Ambuye wawo pa tsikuli. 16. Ndipo
iwo adzalowa ndi kulawa moto ku Gahena. 17. Ndipo
kudzanenedwa kwa iwo kuti: "Chimenechi ndicho chilango
chija munkachinena kuti sichidzakhalako."

18. Iyayi! Ndithudi chiwerengero cha anthu olungama
chimasungidwa mu Illiyyun. 19. Kodi mudzadziwa
bwanji kuti Illiyin wapamwambayo ndi chiyani? 20. Ndi

Buku lochita kulembedwa. 21. Limene limaonedwa ndi
iwo okhawo amene ali kufupi ndi zofuna za Mulungu.
22. Ndithudi anthu onse olungama adzakhala ku malo a
mtendere. 23. Atakhala pa mipando ya wofowofo ndipo ali
kuyang'ana uku ndi uku . 24. Ndipo udzaona chisangalalo
pa nkhope zawo. 25. Iwo adzapatsidwa kuti amwe vinyo
weniweni amene sanatsegulidwepo. 26. Womaliza wake
adzakhala ndi fungo labwino ndipo pachifukwa cha
ichi, aleke onse amene afuna kulimbikira kuti alimbike.
27. Wosakanizidwa ndi madzi a Tasnim. 28. Kasupe amene
anthu odala adzakhala ali kumwa. 29. Ndithudi! Anthu
amene amachita zoipa, anali kuwaseka anthu amene
anakhulupirira. 30. Ndi kumacheulana iwo akamadutsa
pakati pawo. 31. Ndipo iwo amati akabwerera kwa anthu
awo amabwera ali kunyoza. 32. Ndipo amati akawaona iwo
amati: "Ndithudi awa ndiwo anthu osochera." 33. Pamene
iwo sadalamulidwe kuti akhale owayang'anira. 34. Koma pa
tsikuli anthu okhulupirira adzaseka anthu osakhulupirira.
35. Ali pa mipando yawofowofo ndi kumayang'ana.
36. Kodi anthu osakhulupirira, sanalipidwe mphotho yawo
molingana ndi ntchito zawo?

# AL-INSIQAQ

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pamene thambo lidzang'ambika. 2. Ndipo limva ndi
kumvera Ambuye wake ndipo ling'ambikadi. 3. Pamene
nthaka idzatambasulidwa. 4. Ndi kutulutsa zonse zimene
zinakwiriridwa m'kati mwake ndi kukhala yopanda
kanthu. 5. Ndipo limva ndi kumvera Ambuye wake
ndipo ling'ambikadi. 6. Oh iwe munthu! Ndithudi iwe
uli kubwerera kupita kwa Ambuye wako ndi ntchito
zako. Kubwerera kotsimikizidwa. Motero udzakumana
nazo. 7. Koma Iye amene adzapatsidwa Buku lake
m'dzanja lamanja. 8. Adzawerengedwa mosavuta. 9. Ndipo
adzabwerera kwa anthu ake ndi chisangalalo. 10. Koma
iye amene adzapatsidwa buku lake kumbuyo kwake.
11. Iye adzalira . 12. Ndipo akalowa ku moto walawi – lawi ku
Gahena. 13. Ndithudi iye adali wansangala pakati pa anthu
ake. 14. Ndithudi iye anali kuganiza kuti sadzabwerera kwa
Mulungu. 15. Inde! Ndithudi Ambuye wake anali kuona
zonse zimene iye ankachita. 16. Ine ndilumbira pali kufiira
kwa kulowa kwa dzuwa. 17. Ndi pali usiku ndi zonse zimene
umabweretsa mu mdima. 18. Ndi pali mwezi pamene ufika
pa chimake penipeni. 19. Ndipo inu, ndithudi, mudzayenda
kupita kutsogolo, kuchoka apa ndi kufika apo. 20. Kodi ndi
chifukwa chiyani choti iwo alibe chikhulupiriro 21. Ndipo
pamene Korani ili kuwerengedwa kwa iwo sagwa pansi.

22. Iyayi! Koma anthu osakhulupirira amalikana. 23. Ndipo
Mulungu amadziwa zinthu zonse zimene amasonkhanitsa.
24. Choncho auze iwo za chilango chowawa. 25. Kupatula
okhawo amene akhulupirira ndi kumachita ntchito
zabwino, chifukwa iwo ali ndi malipiro opanda malire.

Sura 85 • Al-Burûj

## Al-Buruj

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pali kumwamba kumene kuli nyenyezi zikulu zikulu.
2. Pali tsiku lolonjezedwa. 3. Pali tsiku la umboni ndi tsiku
loperekedwa umboni. 4. Wotemberereredwa anali anthu
amene anakumba ngalande. 5. Imene munali moto woyaka.
6. Pamene akhala moizungulira. 7. Ndipo iwo adachitira
umboni pa zomwe amachitira anthu okhulupirira. 8. Iwo
analibe mlandu wina uliwonse ndi anthuwa kupatula kuti
anali kukhulupirira mwa Mulungu mmodzi yekha, Mwini
mphamvu zonse, Mwini kuyamikidwa. 9. Mwini Ufumu
wakumwamba ndi dziko lapansi! Ndipo Mulungu ndi
mboni pa chilichonse. 10. Ndithudi onse amene adazunza
amuna okhulupirira, ndi akazi okhulupilira ndipo salapa
machimo awo, adzalandira chilango chowawa cha moto
woyaka wa ku Gahena. 11. Ndithu onse amene akhulupirira
ndi kuchita ntchito zabwino adzakhala m'minda imene ili
ndi mitsinje ya madzi oyenda. Kumeneko ndiko kupambana
kwakukulu. 12. Ndithudi chilango cha Ambuye wako ndi

chowawa. 13. Ndithudi Iye ndiye amene amayambitsa
chilengedwe ndipo adzachibwereza patsiku louka kwa
akufa. 14. Ndipo Iye ndi wokhululuka ndi wachikondi
chodzadza. 15. Mwini wake wa Mpando wachifumu,
Wolemekezeka. 16. Iye amachita chimene afuna. 17. Kodi
iwe siudamve za asirikali. 18. A Farao ndi a Thamoud?
19. Iyayi! Koma anthu osakhulupirira amazikana. 20. Ndipo
Mulungu amawazungulira onse. 21. Iyayi! Ili ndi Buku loyera
la Korani. 22. Lolembedwa m'Buku lotetezedwa.

Sura 86 • At-Târi`k

# Tariq

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni chosatha.

1. Pali kumwamba ndi pali Nyenyezi yowala. 2. Kodi
chidzakudziwitsa kuti Nyenyezi yowala ndi chiani? 3. Ndi
Nyenyezi yowala kothobwetsa maso. 4. Ndithudi moyo
uliwonse uli ndi mtetezi wake. 5. Tamulekani munthu
kuti aganize kuti adalengedwa kuchokera ku chiyani!
6. Iye adalengedwa kuchokera ku madzi otuluka. 7. Amene
amatuluka kuchokera pakati pa pfupa la munsana ndi nthiti.
8. Ndithudi Iye ali ndi mphamvu zomudzutsa. 9. Pa tsiku
limene zinthu zobisika zidzayesedwa. 10. Ndipo adzakhala
wopanda mphamvu kapena womuthandiza. 11. Pali mtambo
umene umapereka mvula kawiri kawiri. 12. Ndi pali dziko
lapansi limene limang'ambika. 13. Ndithudi! Awa ndi mawu
amene amasiyanitsa. 14. Si nthabwala ayi. 15. Ndithudi iwo

ali kukonza chiwembu. 16. Ndipo Inenso ndili kukonza
chiwembu. 17. Motero apatse nthawi anthu osakhulupirira.
Ndipo chita nawo mwamtendere pa kanthawi kochepa.

Sura 87 • Al-A`laa

## AL-A'LA

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Lemekeza dzina la Ambuye wako wapamwambamwamba
2. Amene adalenga zonse ndi kuzikonza bwinobwino.
3. Amene adalamula tsogolo lawo ndi kuwatsogolera.
4. Amene amameretsa msipu. 5. Ndipo amausanduliza
kukhala udzu ouma. 6. Tidzakuphunzitsa kulakatula
chivumbulutso chathu ndipo sudzaiwala. 7. Kupatula
chokhacho chimene Mulungu amafuna. Ndithudi Iye
amadziwa chilichonse chooneka ndi chobisika. 8. Ndipo
Ife tidzakufupikitsira, m'njira yaifupi. 9. Motero kumbutsa
mwina chikumbutso chingawathandize. 10. Chikumbutso
chidzalandiridwa ndi iye amene amaopa Mulungu. 11. Koma
munthu wochimwa adzachisiya. 12. Amene adzaponyedwa
mu ng'anjo yamoto ndi kulawa ululu wake. 13. Mmene
iye sadzafa kapena kukhala ndi moyo. 14. Zoonadi iye
amene adziyeretsa adzakhala wopambana. 15. Amene
amakumbukira dzina la Ambuye wake ndipo amapemphera
panthawi yake. 16. Iyayi, koma inu mumasangalala ndi zinthu
za m'moyo uno. 17. Ndipo moyo umene uli nkudza ndi
wabwino ndi wosatha. 18. Ndithudi! Zonsezi zidalembedwa

mu Mabuku akale a Mulungu. 19. Mabuku a Abrahamu ndi
Mose.

Sura 88 • Al-Grhâshiyah

## Al-Ghashiya

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Kodi wamva za chinthu chachikulu chimene chili nkudza?
2. Nkhope zina, patsiku limeneli, zidzachititsidwa manyazi.
3. Pogwira ntchito zotopetsa. 4. Iwo adzalowa kumoto
woyaka. 5. Iwo adzapatsidwa madzi oti amwe kuchokera
kuchitsime cha moto. 6. Sadzakhala ndi chakudya
china koma chiphe cha mtengo waminga. 7. Chimene
sichidzawapatsa thanzi kapena kuthetsa njala. 8. Nkhope
zina, pa tsikuli, zidzakhala zosangalala. 9. Adzakondwa
chifukwa cha ntchito zawo. 10. Atakhala m'minda ya
pamwamba. 11. Kumene iwo sadzamva zoononga kapena
za bodza. 12. Mudzakhala kasupe wa madzi oyenda.
13. Ndi mipando yonyamuka ya wofowofo. 14. Ndi zikho
zomwera zitaikidwa pambali pake. 15. Ndi makushoni
yoikidwa m'mizere. 16. Ndi mikeka yoyalidwa bwino pansi
pake. 17. Kodi iwo saona mmene ngamira zidalengedwera?
18. Ndi Kumwamba mmene kudakwezedwera? 19. Ndi
mapiri mmene adalengedwera mokhazikika? 20. Ndi
dziko mmene adalitambasulira? 21. Motero akumbutse,
chifukwa udindo wako ndi wowakumbutsa. 22. Iwe
sindiwe munthu wowakakamiza ayi. 23. Kupatula iye

amene abwerera m'mbuyo ndi kuyamba kusakhulupirira.
24. Motero Mulungu adzamulanga chilango chachikulu.
25. Ndithudi onse adzabwerera kwa Ife. 26. Ndipo, ndithudi,
chiwerengero cha zochita zawo chidzakhala kwa Ife.

SURA 89 • AL-FAJR

# AL FAJR

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Pali m'mbandakucha. 2. Ndi pali usiku khumi. 3. Pali
chofanana ndi chosiyana. 4. Pali usiku pamene uli nkutha.
5. Ndithudi m'menemu muli umboni wokwanira kwa
anthu a nzeru. 6. Kodi iwe siudaone mmene Ambuye
wako adakhaulitsira anthu a Aad? 7. Amene anali atali atali
ngati nsanamila zitali zitali. 8. Wolingana nawo amene
sanalengedwepo padziko. 9. Ndi anthu a Thamoud,
amene ankakumba nyumba zawo m'miyala ya m'dambo.
10. Ndi Farao, amene anali ndi zichiri. 11. Amene anali
kuphwanya malamulo paliponse m'dziko. 12. Ndipo
adachulukitsa chisokonezo. 13. Motero Ambuye wako
adabweretsa chilango chosiyana siyana chowawa pa iwo.
14. Ndithudi Ambuye wako amaona. 15. Ndipo nthawi zonse
munthu, pamene Ambuye wake amuyesa pomukweza ndi
kumuonetsera chifundo chake, iye amati: "Ambuye wanga
wandilemekeza ine." 16. Koma akamuyesa pomumana
zinthu, iye amati: "Ambuye wanga ali kundizunza ine."
17. Iyayi! Koma inu simuonetsa chifundo kwa ana a masiye.

18. Ndi kuuzana kuti mudzidyetsa anthu osauka. 19. Inu
mumalanda chuma cha anthu opanda mphamvu chifukwa
cha umbombo. 20. Ndipo mumakonda chuma ndi mitima
yanu yonse. 21. Iyayi! Koma pamene dziko lidzasinjidwa
kukhala ufa. 22. Ndipo Ambuye wanu adzadza pamodzi ndi
angelo ali pa mizere. 23. Ndipo Gahena idzabweretsedwa
pafupi patsikuli. Ndipo patsikuli munthu adzakumbukira.
Koma, kodi chikumbumtima chake chidzamuthandiza
motani? 24. Iye adzanena kuti: "Kalanga ine! Ndikanakhala
ndinali kuchita zabwino pamene ndinali ndi moyo."
25. Motero patsikuli, palibe wina amene adzalanga monga
momwe Iye adzalangire. 26. Ndipo palibe wina amene
adzamanga monga ngati momwe Iye adzamangire.
27. Oh! Iwe wokhutitsidwa. 28. Bwerera kwa Ambuye wako
mosangalala ndi Iye, ndi Iye mosangalala ndi iwe. 29. Lowa
m'gulu la akapolo anga wolemekezeka. 30. Ndipo lowa mu
Paradiso yanga.

SURA 90 • AL-BALAD

# AL BALAD

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ine ndili kulumbira pali Mzinda uwu. 2. Ndipo iwe uli ndi
ufulu mu Mzinda uwu. 3. Ndi pali wobereka ndi chimene
adabereka. 4. Ndithudi Ife tidamulenga munthu m'mavuto.
5. Kodi amaganiza kuti palibe wina aliyense amene ali
ndi mphamvu pa iye? 6. Iye amanena monyada kuti: "Ine

ndaononga chuma chambiri.” 7. Kodi iye amaganiza kuti
palibe wina amene ali kumuona? 8. Kodi Ife sitidamupatse
maso awiri? 9. Ndi lirime ndi milomo iwiri. 10. Ndi
kumulangiza iye njira ziwiri? 11. Koma sayerekeza kutsata
njira yozyolika. 12. Kodi chidzakuuza ndi chiani za njira
yozyolika? 13. Ndi kumasula kapolo. 14. Kapena kupereka
chakudya nthawi ya njala. 15. Kwa wamasiye amene
ndi wachinansi. 16. Kapena munthu wosauka, wofuna
chithandizo. 17. Ndipo iye anakhala mmodzi wa anthu
amene akhulupirira, ndipo analangizana wina ndi mzake
kupilira, kumva chisoni ndi kuonetsa chifundo. 18. Iwo
ndiwo amene adzakhala kudzanja lamanja. 19. Koma iwo
amene anakana chivumbulutso chathu, adzaima ku dzanja
lamanzere. 20. Ndipo moto wa ku Gahena udzawakuta iwo.

Sura 91 • A-sh-Shams

# Al-Shams

M’dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pali dzuwa ndi kuwala kwake. 2. Ndi pali mwezi umene
umatuluka dzuwa litalowa. 3. Ndi masana pamene
kumayera . 4. Ndi pali usiku umene umabisa. 5. Ndi pali
Kumwamba ndi Iye amene adakulenga. 6. Ndi pali dziko
lapansi ndi Iye amene analitambasula. 7. Ndi pali mzimu
ndi Iye amene adaulenga. 8. Ndi kumupatsa iye nzeru
zodziwa choipa ndi chabwino. 9. Ndithudi wopambana ndi
amene amadziyeretsa. 10. Ndipo wolephera ndiye amene

wadzidetsa. 11. Anthu a Thamoud adakana Mtumwi wawo
poukira moyerekedwa. 12. Pamene munthu olakwa kwambiri
adayambitsa chipolowe. 13. Ndipo Mthenga wa Mulungu
anati kwa iwo: “Samalirani ngamira ya ikazi ya Mulungu ndi
tsiku lake lomwa madzi!” 14. Iwo sadakhulupirire ayi ndipo
ngamirayo adaipha. Motero Ambuye wawo adawaononga
chifukwa cha machimo awo ndipo adafafaniza onse
mosasankha. 15. Iye sadaope chotsatira chake.

Sura 92 • Al-Layl

## Al-Layl

M’dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. Pali usiku pamene mdima umayamba. 2. Ndi masana pamene
kumayera. 3. Ndi pali Iye amene adalenga chachimuna ndi
chachikazi. 4. Ndithudi zochita zanu zonse zili ndi mapeto
osiyana. 5. Akakhala iye amene amapereka chaulere ndipo
amamuopa Mulungu. 6. Ndipo amakhulupirira pochita
zinthu zabwino. 7. Ife tidzamusalazira njira yake ya ku
chipulumutso. 8. Koma iye amene sapereka chaulere ndipo
amaganiza kuti ndi woima payekha, 9. Sakhulupirira ndipo
sachita ntchito zabwino, 10. Tidzamusalazira njira yake ya
ku chionongeko. 11. Kodi chuma chake chidzamuthandiza
chiani pamene iye azidzazunzika? 12. Ndithudi ndi udindo
wathu kupereka chilangizo. 13. Ndipo, ndithudi, zonse za
m’moyo umene uli nkudza ndi za m’moyo uno ndi zathu.
14. Motero ndakuchenjezani za moto wa lawilawi. 15. Kulibe

munthu amene akapsye nawo kupatula munthu wochita
zoipa. 16. Amene amakana choonadi ndipo safuna kumvera
chenjezo. 17. Koma anthu onse olungama, adzatalikirana
nawo. 18. Amene amapereka chaulere chake poonjezera
kudziyeretsa. 19. Osati chifukwa chakuti afuna kupezako
cholowa ayi. 20. Kupatula ndi cholinga chopeza chisomo
cha Ambuye wake, wapamwamba mwamba. 21. Ndithudi
iye adzasangalala.

Sura 93 • Ad-Dhuha

## Al-Dhuha

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pali usana. 2. Ndi pali usiku pamene ulipo. 3. Ambuye wako
sadakutaye iwe ndiponso sakudana nawe ayi. 4. Ndipo,
ndithudi, moyo umene uli nkudza ndi wabwino kwa iwe
kuposa moyo uno. 5. Ndithudi Ambuye wako adzakupatsa,
ndipo iwe chidzakukondweretsa. 6. Kodi sadakupeze
iwe uli wa masiye ndipo adakupatsa malo okhala? 7. Kodi
sadakupeze uli wosochera ndipo Iye adakutsogolera?
8. Kodi sadakupeze iwe waumphawi ndipo adakulemeretsa?
9. Motero iwe usapondereze pansi mwana wa masiye.
10. Ndipo usapirikitse munthu wopempha. 11. Koma lengeza
chisomo cha a Ambuye wako.

SURA 94 • ASH-SHARH

## AL-INSHIRAH

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. Kodi Ife sitidatsegule chifuwa chako? 2. Ndi kukuchotsa
katundu wako wolemera? 3. Amene amalemetsa msana
wako. 4. Ndipo tidakweza mbiri yako yabwino. 5. Ndithudi
m'mavuto muli chithandizo. 6. Ndithudi m'mavuto muli
chithandizo. 7. Ndipo pamene wamaliza, pembedza
Mulungu. 8. Ndipo dzipereke kwathunthu kwa Ambuye
wako.

SURA 95 • AT-TIN

## AL-TIN

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pali mtengo wa mkuyu ndi mtengo wa azitona. 2. Ndi
pali phiri la Sinai. 3. Ndi pali Mzinda uwu wa mtendere.
4. Ndithudi Ife tidamulenga munthu m'chikombole
chabwino. 5. Ndipo tinamutsitsa kukhala wapansi zedi.
6. Kupatula amene amakhulupirira ndipo amachita ntchito
zabwino, iwo adzalandira mphotho yosatha. 7. Kodi ndi
chiyani, chimene chili kukupangitsani kukana tsiku la
chiweruzo? 8. Kodi Mulungu si woweruza wabwino kuposa
oweruza onse?

# AL-ALAQ

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. Werenga! M'dzina la Ambuye wako amene analenga.
2. Yemwe adalenga munthu kuchokera ku kadontho
kamagazi oundana. 3. Werenga! Ndipo Ambuye wako ndiye
wopereka mowoolowa manja. 4. Amene anaphunzitsa
ndi cholembera. 5. Anaphunzitsa munthu chimene sanali
kuchidziwa. 6. Iyayi! Ndithudi, munthu amalakwa mopyola
muyeso. 7. Chifukwa amaganiza kuti iye ndi oima payekha.
8. Ndithudi! Nonse mudzabwerera kwa Ambuye wanu.
9. Kodi mwamuona munthu amene amaletsa 10. Kapolo
pamene akupemphera? 11. Kodi mwamuona ngati iye
alikutsatira chilangizo chabwino? 12. Kapena kulamulira
machitidwe abwino? 13. Ndiuze ngati iye akana choonadi
ndipo salabadira. 14. Kodi iye sadziwa kuti Mulungu amaona
zinthu zonse? 15. Iyayi! Ngati iye sasiya, Ife tidzamududuluza
pogwira tsitsi la pa mphumi pake. 16. Mphumi yabodza
ndi yochimwa. 17. Ndipo mulekeni iye aitane anzake oti
amuthandize. 18. Ife tidzaitana osunga Gahena. 19. Iyayi!
Usamumvere iye. Gunditsa mphumi yako pansi ndipo idza
pafupi ndi Mulungu.

SURA 97 • AL-'KADR

# AL-QADRI

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Ndithudi tinavumbulutsa ilo mu usiku wamphamvu.
2. Kodi ndi chiyani chimene chingakuuzeni kuti mudziwe
kuti usiku wamphamvu ndi otani? 3. Usiku wamphamvu
ndi wabwino kuposa miyezi chikwi chimodzi. 4. Mu usiku
umenewu Angelo ndi Mzimu, ndi chilolezo cha Mulungu,
amachoka kumwamba ndi kutsika pansi ndi malamulo ake
onse. 5. Mtendere mpaka m'mbandakucha.

SURA 98 • AL-BAYYINA

# AL-BAYYINA

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Iwo amene sakhulupirira a m'gulu la anthu a m'Buku
ndi anthu opembedza mafano, sadzasiya kusakhulupilira
mpaka pamene zizindikiro zooneka zitaperekedwa
kwa iwo. 2. Mtumwi wochokera kwa Mulungu amene
ali kuwerenga kuchokera pa Masamba Oyera. 3. Amene
ali ndi malamulo angwiro ndi omveka bwino ochokera
kwa Mulungu. 4. Ndipo anthu okhulupirira Buku
sanayambe kugawikana pakati pawo mpaka pamene
zizindikiro zooneka zidaperekedwa kwa iwo. 5. Ndipo

iwo sadalamulidwe koma kuti azipembedza Mulungu ndipo kuti asapembedze wina aliyense koma Iye yekha ndipo kuti adzipemphera pa nthawi yake ndi kupereka msonkho wothandiza anthu osauka. Ndipo chimenechi ndicho chipembedzo chabwino. 6. Ndithudi iwo amene sakhulupirira amene ali pakati pa anthu a m'Buku, ndi anthu opembedza mafano, adzakhala ku moto wa ku Gahena. Iwo ndiwo oipa zedi pa zolengedwa zonse. 7. Ndithudi iwo amene atsatira chikhulupiriro choonadi ndipo amachita ntchito zabwino ndiwo olemekezeka pa zolengedwa zonse. 8. Mphotho yawo imene ili ndi Ambuye wawo ndi kuwaika m'minda imene imathiririridwa ndi madzi ya m'mitsinje pansi pake, kumene adzakhalako nthawi zonse. Mulungu ndi wosangalala ndi iwo ndipo nawonso ndi osangalala ndi Iye. M'menemo ndi m'mene munthu oopa Mulungu adzalandirire mphotho yake.

Sura 99 • Az-Zilzâl

# Al-Zalzala

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha.

1. Pamene dziko lidzagwedezeka ndi chivomerezi chomaliza. 2. Ndipo pamene nthaka idzatulutsa katundu amene ali m'kati mwake. 3. Ndipo munthu adzafunsa: "Kodi yatani?" 4. Pa tsikuli nthaka idzaulula zonse. 5. Chifukwa Ambuye wako wayiuza kuti itero. 6. Pa tsikuli mtundu wa anthu udzadza m'magulu osiyana siyana kudzalangizidwa

ntchito zawo. 7. Motero aliyense amene amachita chabwino
cholemera ngati njere ya mpiru, adzachiona. 8. Ndipo
aliyense amene amachita choipa cholemera ngati njere ya
mpiru, adzachiona.

Sura 100 • Al-'Adiyât

# Al-Adiyat

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pali zothamanga kwambiri ndi kupuma kwawo kofulumira.
2. Ndi zimene zimaonetsa moto zikamathamanga. 3. Ndipo
zimachita nkhondo m'mbandakucha. 4. Ndi kuonetsa
fumbi. 5. Ndi kuphwanya pakati gulu la adani. 6. Ndithudi!
Munthu sathokoza kwa Ambuye wake. 7. Ndipo mwini wake
amachitira umboni zimenezi. 8. Ndithudi iye ali kukonda
chuma kwambiri. 9. Kodi iye sadziwa kuti pamene zonse
zili m'manda zidzatulutsidwa ndi kuonetsedwa poyera.
10. Ndi zonse zimene zili m'mitima ya anthu zizidzaululidwa.
11. Ndithudi, patsiku limeneli, Ambuye wako adzakhala ali
kudziwa chilichonse

SURA 101 • AL-'KÂRIYAH

# AL-QARIA

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. Tsiku louka kwa akufa. 2. Kodi tsiku louka kwa akufa
ndi chiyani? 3. Kodi ndi chiyani chimene chidzakuuze iwe
kuti tsiku louka kwa akufa ndi chiani? 4. Ndi tsiku limene
anthu adzakhala ngati dzombe louluka paliponse. 5. Ndi
mapiri adzakhala ngati fumbefumbe za ubweya. 6. Ndipo
iye amene muyeso wake wa ntchito zabwino udzakhala
wolemera. 7. Adzakhala ndi moyo wa chimwemwe ndi
chisangalalo. 8. Koma iye amene muyeso wake wa ntchito
zabwino udzapezeka wopepuka. 9. Mudzi wake udzakhala
dzenje lamoto. 10. Kodi ndi chiyani chimene chidzakuuze
zinthu zonsezi? 11. Ndi moto wa malawi osatha

SURA 102 • AT-TAKÂTHUR

# AL-TAKTHUR

M'dzina la  Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. Mpikisano wosonkhanitsa chuma cha padziko
wakutangwanikitsani inu. 2. Mpaka pamene inu mulowa
m'manda. 3. Iyayi! Inu mudzadziwa! 4. Kachiwiri, Iyayi!
Inu mudzadziwa. 5. Iyayi! Inu mukanadziwa kwenikweni.
6. Ndithudi inu mudzaona moto woyaka. 7. Kachiwiri inu

mudzauona ndi maso anu! 8. Ndipo patsiku limeneli inu mudzafunsidwa za chisangalalo chimene munali kuchita.

Sura 103 • Al-'Asr

## Al-Asr

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha.

1. Pali nthawi. 2. Ndithudi ! Munthu ndi otayika. 3. Kupatula okhawo amene amakhulupirira ndi kuchita ntchito zabwino ndipo amalimbikitsana wina ndi mzake kuchita chilungamo ndi kukumbutsana kupirira.

Sura 104 • Al-Humâzah

## Al-Humaza

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha.

1. Tsoka kwa aliyense amene amajeda ndi kuononga mbiri ya anzake. 2. Amene amasonkhanitsa chuma chake ndi kumachiwerenga . 3. Iye amaganiza kuti chuma chake chidzamuchititsa iye kukhala ndi moyo wamuyaya. 4. Iyayi! Ndithudi iye adzaponyedwa ku moto woononga. 5. Kodi chidzakuuza kuti moto woononga ndi chiyani? 6. Ndi moto wa Mulungu umene Mwini wake anauyatsa. 7. Umene umafuka m'mitima ya anthu. 8. Ndithudi udzawatsekereza mbali iliyonse. 9. M'sanamila zoima.

SURA 105 • AL-FÎL

# AL FIL

M'dzina la Mulungu Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha.

1. Kodi siudaone mmene Mulungu adachitira ndi eni ake
a Njovu? 2. Kodi Iye sadasokoneze chiwembu chawo?
3. Ndipo anatumiza gulu la mbalame lolimbana nawo.
4. Zimene zinawalasa miyala ya moto. 5. Ndipo iwo adaoneka
ngati msipu wodyedwa?

SURA 106 • AL-'KURAYSH

# AL-QURYSH

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Pofuna kuteteza mtundu wa Quraish. 2. Kuti apitirire pa
maulendo nthawi ya Chilimwe ndi m'nthawi ya Chisanu.
3. Motero auzeni kuti azipembedza Ambuye wa Nyumba
ino. 4. Amene wawadyetsa m'masiku a njala ndi kuwachotsa
mantha.

# AL-MAUN

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Kodi wamuona munthu amene amakana kuti kuli tsiku la chiweruzo? 2. Iye ndiye amene amazunza mwana wamasiye. 3. Ndipo sakakamiza anthu ena kuti azidyetsa anthu osauka. 4. Motero tsoka kwa iwo amene amapemphera. 5. Amene salabadira mapemphero awo. 6. Amene amachita zabwino pofuna kuti ena awaone. 7. Ndipo amakana kupereka chaulere.

SURA 108 • AL-KAWTHAR

# AL-KAWTHAR

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Ndithudi takupatsa iwe Mtsinje wa Paradiso. 2. Motero pemphera chifukwa cha Ambuye wako ndipo upereke nsembe. 3. Ndithudi aliyense amene akukwiyitsa iwe adzakhala wopanda choyembekezera.

# Al-Kafiruni

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Nena: Oh! Inu anthu osakhulupirira! 2. Ine sindipembedza chimene inu mupembedza. 3. Ndiponso inu simudzapembedza chimene ine ndipembedza. 4. Ndipo ine sindidzapembedza chimene inu muli kuchipembedza. 5. Ndipo inu simudzapembedza chimene ine ndimapembedza. 6. Kwa inu chipembedzo chanu ndipo kwa ine chipembedzo changa.



# Al-Nasr

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Pamene chithandizo cha Mulungu chidza ndi kupambana. 2. Ndipo uona anthu akulowa m'chipembedzo cha Mulungu mu unyinji wawo. 3. Motero lemekeza Ambuye wako ndipo upemphe chikhululukiro chake. Ndithudi Iye amavomera kulapa ndipo ndi wokhululukira.

# AL-LAHAB

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Aonongeke manja a Abu Lahab, ndipo nayenso
aonongeke! 2. Chuma chake ndi ana ake sizidzamuthandiza
ai. 3. Iye adzalowa m'moto wa lawilawi! 4. Ndipo mkazi
wake amene amanyamula nkhuni. 5. Mkhosi mwake muli
chingwe chopota cha mlaza.



# AL-IKHLAS

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini
Chisoni Chosatha

1. Nena: Iye ndi Mulungu, mmodzi. 2. Mulungu, Mwini
Mphamvu zonse. 3. Iye sabereka ndipo Iye sadaberekedwe.
4. Ndipo palibe wina wofanana naye.

# Al-Falaq

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Nena: "Ine ndifuna kuthawira kwa Ambuye wa
M'mbandakucha. 2. Kuchokera ku zinthu zonyansa zimene
walenga. 3. Ndi kuchokera ku zonyansa za nthawi ya usiku
pamene mdima ufika. 4. Ndi kuchokera ku zonyansa
za anthu a matsenga pamene auzila pfundo. 5. "Ndi ku
zonyansa za munthu wa dumbo pamene achita nsanje."



# Al Anas

M'dzina la Mulungu, Mwini Chifundo ndi Mwini Chisoni Chosatha

1. Nena: "Ine ndifuna kuthawira kwa Ambuye wa anthu. 2.
Mfumu ya anthu. 3. Mulungu wa anthu. 4. Kuchokera ku
zonyansa za kazitape amene amachoka akatha. 5. Amene
amanong'oneza m'mitima mwa anthu. 6. Ya majini ndi
anthu."

Quran ndi Bukhu lomwe linabweretsa uthenga wabwino kwa anthu pamodzi ndi malangizo abwino ochokera kumwamba, uthenga wolimbikitsa kufunika kwa ku zindikila kwa munthu pa umoyo wa uzimu komanso ndi luntha lachibadwidwe.

Bukhu lina lililonse limakhala ndi cholinga ndipo cholinga cha Quran ndi kumudziwitsa Munthu chikonzero cha Mulungu pa za chilengedwe. Zimenezo ndi monga kumuuza Munthu chifukwa chomwe Mulungu analengela Dzikoli.nanga ndicholinga chanji chomwe anamuyikila Munthu padzikoli? Nanga chofunika kuti munthu achite ndi chiyani pa Umoyo umenewu asanamwalire? Nanga adzakumana ndi zotani akadzamwalira?. Chimenechi ndiye cholinga cha Quran kumudziwitsa Munthu komanso ndi kumuongolera panthawi ya umoyo wake mpakana kumathero kwa moyo wake.

Cholinga chachikulu cha Quran ndi Kuwunikira, Kuyandikitsa komanso kupangitsa ubwezi ndi Mulungu, mtendere komanso ndi Uzimu. Quran imagwiritsa ntchito mawu monga tawassum, tadabbur komanso ndi tafakkur zomwe zimasonyeza kuphunzitsa chiphunziro kudzela mukuganiza kozama komanso molingalira zizindikiro za Mulungu zomwe zili mbwembwembwe padziko lapansi pano. Matanthawuzo atsopano a Quran imeneyi komanso kalongosoledwe kazolembedwa zake, zalembedwa posaiwara zolinga zimwezi.

GOODWORD

www.goodwordbooks.com
www.cpsglobal.org

ISBN 978-93-86589-11-8

9 789386 589118